شـشيوا

# MALAMULO OFUNIKIRA KWA MSILAMU

LOTANTHAUZIDWA M'CHICHEWA

www.tafseer.info

M'dzina la Allah, Wachifundochambiri, Wachisoni.

# MAU OYAMBA

بسم الله الرحمن الرحيم

Matamando onse ndi a Allah, madalitso ndi mtendere zikhale pa Bwana wathu, Mneneri wathu komanso Wokondedwa wathu Mtumiki wa Allah. Pambuyo pa izi:

**Zindikira iwe m'bale ndi mlongo wanga wa Chisilamu–Allah akuchitireni chifundo – kuti ndithu zikukakamizidwa pa ife kuphunzira mfundo zinayizi:**

❶ **Yoyamba - Maphunziro:** Uku ndiko kumuzindikira Allah Subhaanahu Wata' aalaa komanso Mneneri Wake (SAW) ndinso kuzindikira chipembedzo cha Chisilamu chifukwa n'kosaloledwa kupembedza Allah popanda maphunziro. Tero amene angachite zimenezo ndiye kuti mapeto ake ndi chisokeretso komanso wafanana ndi Akhristu mu zimenezo.

❷ **Yachiwiri – Kugwira ntchito:** Ndipo amene wazindikira napanda kugwira ntchito, ndiye kuti wafanana ndi Ayuda, chifukwa choti iwowo adazindikira ndipo sadagwire ntchito. Zina mwa zinyego za satana, ndiye kuti, ndithudi amafooketsa ndi kusiya maphunziro pomupatsa munthu ziyangoyango m'mutu mwake kuti ndithu iyeyu akatero akhale ali nacho chowiringula kwa Allah mu umbuli wake. Ndipo iye sakudziwa kuti ndithu amene kwamuthekera kupeza mwayi wophunzira ndipo sadachite, ndiye kuti chowiringula chapezeka pa iye. Awa ndi mapulani a anthu a Noah (AS) ﴿جعلوا أصابعهم في آذانهم واستغشوا ثيابهم﴾ Amaika zala zawo m'makutu mwawo komanso amadzifunditsa nsalu zawo Ndicholinga chakuti pasadzapezeke pa iwo umboni woti uthenga udawafikira.

❸ **Yachitatu - Kuitanira ku maphunzirowo:** Ichi n'chifukwa chakuti anthu ozindikira komanso ofalitsa, iwowo ndi alowam' malo a aneneri. Ndipo ndithu Allah Subhaanahu Wata'aalaa watemberera ana a Israeli chifukwa choti adali asakuletsana ku zoipa zimene azichita, ndithudi n'zoipa ﴿كانوا لا يتناهون عن منكر فعلوه﴾ iwowo zedi zimene iwo adali kuzichita. Ndipo kuchita da'awa ndi kuphunzitsa ndi fardh kifaayat, ngati ataimirira kuchita izi amene angakwanitse, ndiye kuti palibe ndi m'modzi yemwe angapeze machismo ndipo ngati onse ataleka nazisiya, ndiye kuti onsewo apeza machimo.

❹ **Yachinayi -Kupirira pa masautso:** Kukhalepo pophunzira maphunziro ndipowagwiritsa ntchito komanso poitanira ku maphunzirowo.

**Ndipo potenga nawo mbali kochokera kwa ife pochotsa umbuli, ndikufewetsera pofunafuna maphunziro, tasonkhanitsa mu buku lachidule ili zina mwa zomwe zingapezeke nalo kukwaniritsa mu maphunziro a Shariat limodzi ndi majuzu atatu omaliza a Qur'aan Yolemekezeka ndi ndemanga zake chifukwa chochuluka kubwerezabwereza kwake ndipo (Zomwe sizingapezeke zonse, sizisiidwa zambiri zake).**

Ndipo ife tachita khama mu zimenezi zonsezi pochita chidule ndi zomwe zatsimikizika zochokera kwa Mneneri (SAW). Ndipo ife sitikudzigunda pa mtima kuti ndithudi tafikira kukwanirira, popeza kutero ndi zinthu zomwe wadzisankhira Allah Subhaanahu Wata'aalaa kwa Iye Mwini, koma ili ndi khama la munthu wochepekedwa. Ngati zili zolondola, ndiye kuti zachokera kwa Allah koma zikakhala zolakwika, ndiye kuti zachokera kwa ife tokha ndi satana, kotero Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) atalikirana ndi zimenezo. Ndipo Allah amuchitire chifundo munthu aliyense yemwe wapereka mphatso kwa ife ya zolakwika zathu kudzera mu kudzudzula kwa cholinga komwe kuli komanga. Tikumupempha Allah kuti alipire aliyense amene watenga nawo mbali polikonza bukuli, kulisindikiza, kuligawa, kuliwerenga ndi kuliphunzitsa. Malipiro abwino ndikuti alandire zimenezo kuchokera kwa iwo komanso awachulukitsire iwowo malipiro ndi zopatsidwa.

**Ndipo Allah ndi amene ali Wozindikiritsitsa, ndipo madalitso ndi mtendere zikhale pa Bwana wathu komanso Mneneri wathu Muhammad, komanso a kubanja lake ndi ophunzira ake onse.**

www.tafseer.info shesh@tafseer.info

| | |
|---|---|
| 1. UBWINO WA KUWERENGA QUR'AN | 2 |
| 2. MALAMULO OFUNIKIRA KWA MSILAMU | 4 |
| 3. MAFUNSO OFUNIKA MU UMOYO WA MSILAMU | 97 |
| 4. NTCHITO ZA MITIMA | 118 |
| 5. KUKAMBIRANA MWACHIFATSE | 130 |
| 6. UMBONI WONENA KUTI PALIBE WOPEMBEDZEDWA MWA CHOONADI KOMA ALLAH | 147 |
| 7. UMBONI WONENA KUTI MUHAMMAD NDI MTUMIKI WA ALLAH | 149 |
| 8. TWAHARAH | 151 |
| 9. MALAMULO AMAYI | 157 |
| 10. MAYI M'CHISILAMU | 160 |
| 11. SWALAAT | 165 |
| 12. ZAKAAT | 173 |
| 13. SWAUM (KUSALA) | 177 |
| 14. HAJJ NDI UMRAT | 181 |
| 15. MAPHINDU OSIYANASIYANA | 187 |
| 16. MADUAA A SHARIAT | 193 |
| 17. DU'AA (PEMPHERO) | 200 |
| 18. MADUAA OFUNIKA OYENERA KUWASUNGA | 202 |
| 19. MALONDA APHINDU | 208 |
| 20. MA DU'AA A M'MAWA NDI MADZULO PA TSIKU LILI LONSE | 209 |
| 21. ZOYANKHULA NDI ZOCHITIKA ZOMWE ZANENEDWA KUTI ZILI NDI MALIPIRO AKULU | 212 |
| 22. ZINTHU ZOMWE KWAFIKA KULETSEDWA KU ZIMENEZO KOMANSO KUZICHITA | 220 |
| 23. ULENDO WAMUYAYA NJIRA YAKO YA KU JANNAT KAPENA KUMOTO | 225 |
| 24. KACHITIDWE KA WUDHU | |
| 25. KASWALIDWE KA SWALAAT | |
| 26. ILM IMAFUNIKA KUIGWIRITSIRA NTCHITO | |

# UBWINO WA KUWERENGA QUR'AN

Kutamandidwa konse ndi kwa Allah, ndipo madalitso ndi mtendere zikhale pa Bwana wathu wokondedwa, Mtumiki wathu Muhammad (SAW), komanso pa akunyumba ake ndi Maswahaaba ake. Pambuyo pa zonsezi; tikutsimikiza kuti Quràn ndi mau a Allah, ndipo kupambana kwake pamwamba pa mau ena alionse kuli ngati kupambana kwa Allah pa zolengedwa Zake, komanso kuwerengedwa kwake nkopambana kwambiri pa zomwe lilime lingayankhule.

**UBWINO WA KUPHUNZIRA QURAN, KUPHUNZITSA NDI KUIWERENGA**

- **MALIPIRO A KUIPHUNZITSA: (i)** Mtumiki (SAW) anati: "*Wopambana mwa inu ndi amene anaphunzira Qur'an naiphunzitsa*." (Bukhaar).

**(ii)** Mtumiki Muhammad (SAW) anatinso: "*Munthu amene waphunzitsa Ayat (ndime) imodzi ya Buku la Allah (Quran) amakhala nawo malipiro ake monga muli monse mmene ingamawerengedwere* (ndi anthu amene adawaphunzitsa aja)."

- **MALIPIRO A KUIWERENGA:** Mtumiki (SAW) anati: "*Amene angawerenge chilembo chimodzi kuchokera m'buku la Allah ndi chilembocho adzakhala ndi sawabu imodzi, ndipo sawabu imodziyo adzapezanso sawabu khumi zofanana ndi iyo*." (Tirmidhi).

**Adanena Ibn Rajab** (RA) kuti: " Kuwonjezera kwa sawab imodzi ndi sawabu khumi zonga imeneyi kukuyenerera kukhala pa zabwino zonse. Chomwe chikusonyeza izi ndi kuyankhula kwa Allah kwakuti: [Amene adzabwere ndi chabwino chimodzi adzapeza khumi zofanana ndi chabwino chimodzi chija]. Tsono kuwonjezera pa sawabu khumizi kumakhala malinga ndi kwa amene Allah wafuna kumuwonjezera. Kuwonjezeraku kumafika mpaka zowonjezera zikwi zisanu ndi ziwiri (700 ) ndikumapitirira apo. Kuwonjezeraku – pambuyo pa ubwino ndi madalitso a Allah, kumakhala chifukwa chakuopa kwa mtima, kuiganizira mozama, kumva matanthauzo ake ndi zina zonga izo.

**MAWERENGEDWE A QURAN**

- Kuwerenga Quran komanso kutchula dzina la Allah pa Swalaatat kapena pena paliponse sikutengedwa kuti watero pokhapokha munthu atazitchula kwenikweni ziwirizi pamulingo wodzimva mwini wakeyo mopanda kusokoneza anthu ena.
- Ayenera kumaiwerenga mwapang'onopan'ono. Atafunsidwa Anas (RA) zakawerengedwe ka Mtumiki (SAW), poyankha adanena kuti: '*Ankakoka kwambiri pakuwerenga mau oti : Bismillah, komanso Al -Rahmaan ndi mau oti Al- Raheem*.' (Bukhaar)

**MULINGO WA KUWERENGA QURAN**

Maswahaaba a Mtumiki (SAW) ankadziikira gawo la kuwerenga Quran tsiku lili lonse. Palibe mmodzi wa iwo amene adadzizoloweza kuimaliza m'masiku ochepera asanu ndi awiri (7). Kungoti kwafika chiletso choimaliza m'masiku ochepra atatu (3).

**KUWERENGA QURAN KOCHOKERA M'MUTU** Kukakhala kwa amene akuwerenga Quran kochokera m'mutu mwake monga mmene adailowezera mukupezekamo kulingalira mofatsa ndi mozama komanso kusonkhanitsa kwa mtima ndi maso kuposa momwe adakaiwerengera mu Mushaf, kungakhale kuwerenga koteroko kopambana. Ziwirizi zikakhala mwa munthu pamulingo wofanana ndiye kuti kuwerenga kochokera mu Mushaf nkopambana.

**LANGIZO** Choncho m'bale wanga wolemekezeka, ukhale ndi khama logwiritsa ntchito nthawi yako powerenga Qur'an, ndipo udzisankhire gawo lowerenga pa tsiku lili lonse, usalisiye gawolo zingavute maka ndipo chaching'ono chopitirira ndichabwino kwambiri kuposa chambiri chodukiza. Utati waiwala kapena wagona usanawerenge gawo lako, mawa lake ubweze. Mtumiki (SAW) anati: "*Munthu amene wagona atasiya gawo lakuwerenga kwake kwa Quran, kapena wasiya kena kake m'gawolo, ndipo naliwerenga munthawi ya pakati pa Swalaatat ya Fajr ndi Zuhr, adzalipidwa malipiro kukhala ngati wawerenga nthawi ya usiku*." (Muslim.)

Usakhale m'gulu la anthu amene aisiya Qur'an ndi kuiyiwala mwa mtundu wina ulionse, monga kusiya kuiwerenga, kapena kuilakatula, kapena kuilingalira, kapena kuigwiritsa ntchito, kapena kufuna machilitso ndi iyo.

**UBWINO WA KUPHUNZIRA QUR'AN, KUILOWEZA PA MTIMA NDI KUKHALA NDI UKADAULO PA KAWERENGEDWE**

Mtumiki (SAW) anati: "*Munthu amene akuwerenga Qur'an iye ataisunga pa mtima adzakhala ndi Angero Olemekezeka abwino (patsiku la Kiyama), ndipo amene amawerenga Qur'an moisamala kumachita kuti ikumuvuta adzalandira malipiro awiri*." ((Bukhaar) - Muslim.)

Ananenanso Mtumiki (SAW) kuti: "*Kudzanenedwa kwa amene amawerenga Qur'an kuti: 'Werenga ndipo kwera komanso ulakatule monga momwe unkalakatulira pa dziko la pansi, chifukwa malo ako ali kumapeto kwa Ayah yomwe umalizire kuwerenga*.'" (Tirmidhi)

**Sheikh Alkhattwaabi (RA) ananena kuti:** "Zadza mu zoyankhula za Maswahaaba kuti chiwerengero cha ma Aayah a Qur'an chili molingana ndi magawo a Jannah, kotero kuti adzauzidwa wowerenga Qur'an kuti kwera pa gawo la Jannah molingana ndi m'mene unkawerengera ma Aayah a Qur'an, choncho amene wakwanitsa kuwerenga Qur'an yonse akakhala pa gawo la mapeto wopambana la Jannah ku Aakhirah, ndipo amene wawerenga gawo limodzi la Qur'an, kukwera kwake sitepe kudzakhala molingana ndi gawolo; choncho mapeto a sawabu adzakhala pa mathero a kuwerenga."

**MALIPIRO A MUNTHU AMENE MWANA WAKE WAPHUNZIRA QUR'AN**

Adanena Mtumiki (SAW) kuti : "*Amene wawerenga Qur'an ndikuiphunzira komanso nkuigwiritsira ntchito, tsiku la Kiyama makolo ake awiriwo adzavekedwa kumutu kwawo nduwira yowala ngati dzuwa, komanso adzavekedwa masuti osafanana ndi a dziko lapansi, ndipo makolo awiriwo adzanena kuti : 'nchifukwa chiyani tavekedwa zimenezi?' Ndipo kudzanenedwa kuti : 'ndi chifukwa cha kuphunzira Qur'an kwa mwana wanu*." (Haakim)

**PEMPHO LA QUR'AN PA TSIKU LOMALIZA KUMPEMPHERERA AMENE AMAIWERENGA** Mtumiki (SAW) anati: " *Muziiwerenga Qur'an pakuti iyo idzafika tsiku la Kiyama pamaso pa Allah ikumudandaulira wowerenga Qur'ani yo kuti Allah amukhululukire*." (Muslim.). Ananenanso Mtumiki (SAW) kuti: "*Swaum (kusala chakudya m'mwezi wa Ramadhaan) ndi Qur'an zikadandaula pa maso pa Allah kuti amukhululukire kapolo Wake pa tsiku la Kiyama*." (Ahmad, Haakim.)

**MALIPIRO A ANTHU AMENE ASONKHANA KUTI AZIWERENGA QUR'AN NDIKUMAPHUNZITSANA**

Mtumiki (SAW) anati: "*Sangasonkhane anthu m'nyumba imodzi mwa nyumba za Allah akuwerenga Buku Lake ndikumaphunzitsana pakati pawo, pokhapokha madalitso amawatsikira pa iwo, chisomo cha Allah chimawaphimba ndipo angero amawakuta, komanso Allah amawatchula iwo m'gulu la amene ali pafupi Naye*." (Abu Dawood.)

**MIYAMBO YA KUWERENGA QUR'AN**

Imaam Ibn Katheer (RA) watchula miyambo ingapo, ndipo ina mwa iyo ndi iyi: Asaikhudze komanso asaiwerenge Qur'an pokhapokha iye ali ndi twahara. Agwiritse ntchito miswaki, avale zovala zake zabwino, alunjike ku Qiblah, asiyize kaye kuwerenga Qur'an akafuna kuyasamula, asadukize kuwerenga potchula mau ena pokhapokha patakhala chifukwa chokwanira, aikire maganizo ake powerenga Qur'an, aime pa Ayah yomwe ikulonjeza za mtendere wa Allah ndikupempha (mtenderewo), ndikuimanso pa Ayah yomwe ikunena za chilango ndikupempha chitetezo cha Allah, asausiye Muahaf uli wovundukulidwa ndiponso asaike kanthu kena kake pamwamba pake, ena mwa iwo asakweze mau powerenga Qur'an kuposa anzawo, asawerenge Qur'an m'misika ndi m'malo momwe mukuchitika phokoso.

# SUURATUL FAATIHAH

M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.

(1) Surataul Faatihah; idatchedwa Suurat imeneneyi kuti "Alfaatiihah" chifukwa ndi imene imatsekulira Qur'aan Yolemekezeka. Imatchedwanso kuti "Almathaani" chifukwa choti imawerengedwa mu rakat iliyonse. Komanso Suratyi ili ndi maina ena.

Ndikuyamba kuwerenga Qur'aan ndi dzina la Allah mopempha chithandizo kwa Iye. "Allah" ndi puropala nauni la Mbuye Amene ali wapamwambamwamba Wopembedzedwa mwachoonadi kuleka wina aliyense wosakhala Iye. Limeneneli ndi dzina lapaderadera la Allah ndipo sangatchedwe nalo wina aliyense. (Al-Rahmaan)- Mwini chifundo chokwana, Amene chifundo Chake chakwanira zolengedwa Zake zonse mosasiyanitsa. (Al-Raheem) Wachisoni ndi anthu okhulupirira. Awiriwa ndi maina awiri mu maina Ake Iye Wapamwambamwamba, mainawa akupereka tanthauzo lotsimikizira mbiri ya chisoni kwa Allah Taalaa chomwe chili choyenerera ndi ukulu Wake.

(2) Matamando onse ndi a Allah Mbuye wa zolengedwa zonse.

[Kutamandika konse ndi kwa Allah ndi mbiri Zake zonse zomwe zili mbiri za uchikwanekwane, ndi mautendere Ake owonekera komanso obisika a chipembedzo komanso a za dziko. Mkatikati mwa mawu amenewa muli lamulo lompembedza Iye ndikuti adzimuthokoza. Iye Yekhayo ndiwoyenerera zimenezo ndipo Iye Subhaanahu ndi amene adalenga zolengedwa zonse. Iye ndi Amene amaimirira popereka zosoweka zawo. Iye ndi Mleri wa zolengedwa Zake zonse pozipatsa mtendere Wake komanso powaninkha abwenzi Ake chikhulupiriro ndi ntchito zabwino.]

(3) Wachifundo chambiri Wachisoni.

[Wachifundo chambiri amene chisoni Chake chafikira zolengedwa zonse. Wachisoni chowachitira anthu okhulupirira. Awiriwa ndi maina mu maina a Allah Taala.]

(4) Mwini wa tsiku la malipiro [Iye Yekhayo subhaanahu ndi mwini wa tsiku la Qiyaamah lomwe ndi tsiku la malipiro a ntchito zonse. Mu kuwerenga kwa Msilamu kwa Ayat imeneyi mu rakaat ili yonse ya Swalaat yake muli chikumbutso kwa iye cha Tsiku Lomaliza, komanso kumupatsa mphamvu iye zokonzekera ntchito zabwino ndi kusiya machimo ndi zoipa.]

(5) Inu Nokha tikukupembedzani komanso Inu Nokha tikukupemphani thandizo.

[Ife tikukulunjikani Inu Nokha pokuchitirani

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ ﴿١﴾
ٱلۡحَمۡدُ لِلَّهِ رَبِّ ٱلۡعَٰلَمِينَ ﴿٢﴾ ٱلرَّحۡمَٰنِ
ٱلرَّحِيمِ ﴿٣﴾ مَٰلِكِ يَوۡمِ ٱلدِّينِ ﴿٤﴾ إِيَّاكَ نَعۡبُدُ وَإِيَّاكَ
نَسۡتَعِينُ ﴿٥﴾ ٱهۡدِنَا ٱلصِّرَٰطَ ٱلۡمُسۡتَقِيمَ ﴿٦﴾
صِرَٰطَ ٱلَّذِينَ أَنۡعَمۡتَ عَلَيۡهِمۡ غَيۡرِ ٱلۡمَغۡضُوبِ
عَلَيۡهِمۡ وَلَا ٱلضَّآلِّينَ ﴿٧﴾

Ibaadat komanso tikupempha thandizo kudzera mwa Inu Nokha mu zinthu zathu zonse. Zonse zili m'manja Mwanu. Palibe amene angakhale nako ngakhale kachinthu kochepetsetsa ngati mbewu yampiru mwa zimenezo. Ndipo mu ayat imeneyi muli umboni woti nkosavomerezeka kwa kapolo kupereka kanthu kena kali konse ka ibaadat monga duwaa, kupempha chipulumutso, kuzinga komanso kuchita twawaaf (kuzungulira nyumba ya kaaba) kupatula kwa Allah Yekhayo. Mu ayat imeneyi mulinso machiritso a mitima ku nthenda yakudzilumikiza ku zinthu zina zosakhala Allah komanso ku matenda a uchiphamaso, kudzikonda komanso kudzikuza.]

(6) Tiwongolereni ife njira yowongoka.

[Tisonyezeni ndikutiwongolera komanso kutipatsa kuthekera kwa kuidziwa njira yowongoka ndipo tilimbikitseni pa imeneyo kufikira tidzakumane Nanu. Njira imeneyi ndiyo Chisilamu chomwe ndi njira yowoneka poyera yomufikitsa munthu ku chiyanjo cha Allah komanso jannat Yake. Njira imeneyi ndi imene adayisonyeza Womaliza wa Atumiki ndi Aneneri Ake (SW), Muhammad (SAW). Choncho palibe njira ina yoti nkumusangalatsa nayo kapolo kupatula pokhazikika pa imemeyi.]

(7) Njira ya anthu amene mudawapatsa mtendere, osati ya amene adakwiyiridwa kapena ya amene adasokera.

[Njira ya anthu amene mudawapatsa mtendere mu gulu la Aneneri komanso ovomereza chowonadi, mashahidi ndi ochita zabwino. Iwowa ndi anthu a chiongoko ndikukhazikika pachiongokopo. Ndipo musatichite mu gulu la anthu amene ayenda mu njira za omwe adakwiyiridwa. Awa ndi anthu amene adadziwa chowonadi napanda kuchigwiritsira ntchito, amenewa ndi Ayuda komanso anthu ena amene

سُورَةُ المُجَادلَة

ترتيبها ٥٨ — آياتها ٢٢

بِسْمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحْمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

قَدْ سَمِعَ ٱللَّهُ قَوْلَ ٱلَّتِى تُجَٰدِلُكَ فِى زَوْجِهَا وَتَشْتَكِىٓ إِلَى ٱللَّهِ
وَٱللَّهُ يَسْمَعُ تَحَاوُرَكُمَآ ۚ إِنَّ ٱللَّهَ سَمِيعٌۢ بَصِيرٌ ﴿١﴾ ٱلَّذِينَ يُظَٰهِرُونَ
مِنكُم مِّن نِّسَآئِهِم مَّا هُنَّ أُمَّهَٰتِهِمْ ۖ إِنْ أُمَّهَٰتُهُمْ إِلَّا ٱلَّٰٓـِٔى
وَلَدْنَهُمْ ۚ وَإِنَّهُمْ لَيَقُولُونَ مُنكَرًا مِّنَ ٱلْقَوْلِ وَزُورًا ۚ وَإِنَّ
ٱللَّهَ لَعَفُوٌّ غَفُورٌ ﴿٢﴾ وَٱلَّذِينَ يُظَٰهِرُونَ مِن نِّسَآئِهِمْ ثُمَّ يَعُودُونَ
لِمَا قَالُوا۟ فَتَحْرِيرُ رَقَبَةٍ مِّن قَبْلِ أَن يَتَمَآسَّا ۚ ذَٰلِكُمْ تُوعَظُونَ
بِهِۦ ۚ وَٱللَّهُ بِمَا تَعْمَلُونَ خَبِيرٌ ﴿٣﴾ فَمَن لَّمْ يَجِدْ فَصِيَامُ شَهْرَيْنِ
مُتَتَابِعَيْنِ مِن قَبْلِ أَن يَتَمَآسَّا ۖ فَمَن لَّمْ يَسْتَطِعْ فَإِطْعَامُ سِتِّينَ
مِسْكِينًا ۚ ذَٰلِكَ لِتُؤْمِنُوا۟ بِٱللَّهِ وَرَسُولِهِۦ ۚ وَتِلْكَ حُدُودُ ٱللَّهِ ۗ
وَلِلْكَٰفِرِينَ عَذَابٌ أَلِيمٌ ﴿٤﴾ إِنَّ ٱلَّذِينَ يُحَآدُّونَ ٱللَّهَ وَرَسُولَهُۥ كُبِتُوا۟
كَمَا كُبِتَ ٱلَّذِينَ مِن قَبْلِهِمْ ۚ وَقَدْ أَنزَلْنَآ ءَايَٰتٍۭ بَيِّنَٰتٍ ۚ وَلِلْكَٰفِرِينَ
عَذَابٌ مُّهِينٌ ﴿٥﴾ يَوْمَ يَبْعَثُهُمُ ٱللَّهُ جَمِيعًا فَيُنَبِّئُهُم بِمَا
عَمِلُوٓا۟ ۚ أَحْصَىٰهُ ٱللَّهُ وَنَسُوهُ ۚ وَٱللَّهُ عَلَىٰ كُلِّ شَىْءٍ شَهِيدٌ ﴿٦﴾

akuchita zinthu zofanana ndi iwo. Tsono osokera amenewo ndi anthu amene sadawongoke ndipo adasokera njira. Iwowo ndi Akhristu ndi amene akutsata njira zawo. Mu pempho limeneli muli machiritso a mtima wa Msilamu a nthenda ya kukanira, umbuli ndi kusokera. Komanso muli chisonyezo choti ndithu mtenedre waukulu kwambiri kuposa wina uli wonse ndi mtendere wa Chisilamu. Amene akudziwitsitsa bwino chowonadi ndikuchitsata akhala woyenerera kuipeza njira yowongoka. Palibe chikaiko chiri chonse kuti ndithu Maswahaaba a Mtumiki (SAW) ndi anthu oyenerera kwambiri kupeza zimenezi pambuyo pa Atumiki (AS). Choncho ayat imeneyi yasonyeza ubwino wawo ndikukula kwa ulemerero wawo (RA). Zili bwino kwa wowerenga kunena pa swalaat pambuyo powerenga Alfaatihat kuti : (Aameen) ndipo tanthauzo lake: Oh Ambuye! Tiyankheni. Imeneyi si Ayat ya mu Suratul Fatihah malinga ndi mgwirizano wa maUlmaa. Pachifukwa chimemechi adagwirizana kusailemba mu Msahafu.]

## (58) SURAT-UL- MUJAADALAH

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 (1) Ndithu Allah wamva mawu a (mkazi) amene akubwezeranabwezerana nawe (mawu) pa za mwamuna wake (amene adamsala). Ndipo akusuma kwa Allah. Ndipo Allah akumva kukambirana kwanu. Ndithu Allah Ngwakumva, Ngopenya chilichonse.

[Ndthu Allah wamva mawu a Khaulat Binti Thaalabat amene adakambirana ndi Mtumiki (SAW) pa nkhani ya mwamuna wake Aws Bin Alswaamit mu zinthu zimene zidachoka kwa mwamunayo zomusala mkaziyu. Kumeneko ndikulankhula kwake kwa iye koti: "Iwe kwa ine uli ngati msana wa mayi anga" kutanthauza posavomerezedwa kuchita naye ukwati, uku mkaziyu akumupempha Allah modzichepetsa kuti amuchotsere vuto lakeli. Ndipo Allah akumva kuyankhulana kwanu awirinu, komanso kubwezeranabwezerana kwanu mawu. Ndithu Allah Ngwakumva liwu lili lonse, Woyang'ana chilichonse, palibe chimene chingabisike kwa iye.]

2 (2) Amene akulumbira mwa inu (Asilamu) kusala akazi awo (powafanizira ndi amayi awo). Iwo si amayi awo. Amayi awo ndi amene adawabereka. Ndithu iwo akunena mawu oipa ndiponso onama. Ndipo ndithu Allah Ngofafaniza machimo Ngokhululuka.

[Amene akusala akazi awo mwa inu nkumanena kwa mkazi wake kuti: "Iwe kwa ine uli ngati msana wa mayi anga" kutanthauza kuletsedwa kochita naye ukwati. Oterewo anyoza Allah ndipo asemphanitsa malamulo. Ndipo akazi awowo mwachoonadi sindiwo amayi awo, ndithudi iwowo ndi akazi awo. Amayi awo sali ena kupatula amene adawabala. Ndithu awa amene akusala akazi awowa akunena liwu labodza loipitsitsa losadziwika kuwona kwake. Ndithu Allah Ndiwofafaniza komanso Wokhululuka kwa amene kwachokera zinthu zina zosemphana ndi malamulo, nalapa kulapa koona mtima.]

3 (3) Amene akufanizira akazi awo ndi amayi awo kenako ndikufuna kubwererana nawo poleka zija adanena, apereke ufulu kwa kapolo, asanakhale malo amodzi (ndi mkaziyo). Amenewa ndi malamulo a Allah kwa inu (amene) mukuchenjezedwa nawo. Ndipo Allah akudziwa zimene mukuchita (zoonekera poyera ndi zosaonekera choncho sungani malamulo amene Allah wakhazikitsa pa inu.)

[Ndipo anthu amene akudziletsa kukhalirana

malo amodzi ndi akazi awo, kenako nabwerera kusiya mawu awowo, ndikutsimikiza zakukhalirana nawo malo amodzi akazi awowo; zakakamizidwa kwa mwamuna wosala mkazi wakeyo kupereka dipo lodziletsera. Dipoli ndilo kupereka ufulu kwa kapolo waChisilamu wamwamuna kapena wamkazi asadakhalire naye malo amodzi mkazi wake amene adamusalayo. Limeneli ndilo lamulo la Allah limene mukulangizidwa nalo kwa yemwe wasala mkazi wake, e, inu amene mudakhulupirira! Zili dero ndicholinga choti musamagwere mukusala akazi anu ndikunena bodza, ndikuti mupereke dipo mutagwera m'menemo, ndikutinso musadzaonjezenso kutero. Ndipo kwa Allah sikabisika kali konse mu ntchito zanu, ndipo Iye ndi Amene adzakulipirani pa zimenezo.]

(4) Ndipo amene sadapeze (kapolo) amange swawmu miyezi iwiri yondondozana asadakhalirane pamodzi (ndi mkaziyo), koma amene sadathe kumanga adyetse masikini makumi asanu ndi limodzi. Malamulo amenewa aikidwa kuti mukhulupirire mwa Allah ndi Mtumiki Wake (SAW). Amenewo ndiwo malire a Allah (malamulo okhazikitsidwa ndi Allah choncho musawalumphe). Ndipo chilango chopweteka chili pa osakhulupirira.

[Ndipo amene sadapeze kapolo woti nkumupatsa ufulu, zakakamizidwa kwa iye kumanga miyezi iwiri yondondozana asadakhalire malo amodzi ndi mkazi wakeyo. Ndipo amene sadathe kutero pachifukwa cha pa chilamulo cha sharia, zakakamizidwa kwa iye kudyetsa masikini makumi asanu ndi limodzi chakudya chowakhuthitsa. Zimene talongosolazi kwa inu, za malamulo a Dhihaar, ndi chifukwa choti inu mumuvomereze Allah ndikutsatira Mtumiki Wake (SAW) ndikugwiritsa ntchito zimene wakulamulani ndikuti musiye zimene munkachita nthawi ya umbuli wanu. Ndipo malamulo amene atchulidwawa ndi malamulo a Allah komanso malire Ake choncho musawapyole. Kwa amene akukanira zimenezi ali nacho chilango chowawa.]

4 (5) Ndithu amene akutsutsana ndi Allah kudzanso Mtumiki Wake (SAW), ayalutsidwa monga m'mene adayalutsidwira omwe adalipo patsogolo pawo. Ndithu tatsitsa zisonyezo zoonekera poyera zolongosola momveka (pazololedwa ndi zoletsedwa). Ndipo chilango choyalutsa chili pa osakhulupirira. [Ndithu anthu amene akutsutsana ndi Allah kudzanso Mtumiki Wake (SAW) n'kumasemphanitsa malamulo awo, asiyidwa komanso kuyalutsidwa monga m'mene adasiidwira anthu amene adadza patsogolo pawo iwo asadadze mu magulu amene adatsutsana ndi Allah komanso Atumiki Ake. Ndithudi Ife tatumiza ma ayat omveka bwino pa mtsutso wina uli wonse posonyeza kuti malamulo a Allah ndi malire Ake ndiwo owona, ndikuti amene akukanira ma ayat amenewo, ali nacho chilango choyalutsa ku Jahannama.]

(6) (Kumbuka) tsiku limene Allah adzaukitsa akufa onse ndi kuwafotokozera zimene adachita (pa moyo wa dziko lapansi: zoipa ndi zabwino; Allah) adazisunga mozilemba koma iwo adaziyiwala. Allah ndi mboni ya zonse (palibe chingabisike kwa Iye).

[Ndipo kumbuka iwe Mtumiki (SAW) Tsiku Lakiyama; tsiku limene Allah adzadzutse anthu akufa onse, ndikuwasonkhanitsa oyambirira onse, komanso omalizira pa nthaka imodzi ndikuwauza zimene adachita zabwino kapena zoipa. Allah adazisunga ndikuzilemba mu "Allahuhul Mahfuuz" (kaundula wosungidwa) ndiponso adawasungira iwowo mu mabuku a ntchito zawo pomwe iwo adaziiwala. Ndipo Allah amaona chinthu china chili chonse palibe chimene chingabisike kwa Iye.]

(7) Kodi siukudziwa (iwe, womvera wanzeru) kuti Allah akudziwa za kumwamba ndi za m'dziko lapansi? Sipakhala manong'onong'o a (anthu) atatu koma Iye ngwachinayi wawo. (ndi kudziwa Kwake kosabisika chili chonse cha kumwamba ndi m'dziko); sangakhale (anthu) asanu koma Iye ngwachisanu ndi chimodzi wawo (m'kudziwa Kwake) sangakhale ali ochepera kapena ochulukira koma Iye ali nawo paliponse pomwe ati akhale (Allah ali nawo pamodzi mukudziwa Kwake kosabisika chilichonse), kenako adzawafotokozera pa tsiku lachiweruzo zimene adachita; ndithu, Allah Ngodziwa chilichonse mokwanira.

[Kodi iwe Mtumiki (SAW) siukudziwa kuti Allah Taalaa amadziwa chinthu chili chonse mu thambo zonse komanso mu nthaka? Palibe pomwe akunong'onezana anthu atatu mu zolengedwa Zake nkhani yachibisibisi, pokhapokha Iye amakhala wachinayi wawo mukuzindikira Kwake komanso ndikudziwitsitsa Kwake kwa mbali zonse ya zinthu. Komanso sangakhale asanu pokhapokha Iye amakhala wachisanu n'chimodzi wawo.Ngakhale ochepera pa chiwerengero chatchulidwachi kapena kuchulukirapo kuposa apa pokhapokha Iye amakhala nawo mwa

أَلَمْ تَرَ أَنَّ ٱللَّهَ يَعْلَمُ مَا فِي ٱلسَّمَٰوَٰتِ وَمَا فِي ٱلْأَرْضِ مَا يَكُونُ
مِن نَّجْوَىٰ ثَلَٰثَةٍ إِلَّا هُوَ رَابِعُهُمْ وَلَا خَمْسَةٍ إِلَّا هُوَ سَادِسُهُمْ
وَلَآ أَدْنَىٰ مِن ذَٰلِكَ وَلَآ أَكْثَرَ إِلَّا هُوَ مَعَهُمْ أَيْنَ مَا كَانُوا۟ ثُمَّ يُنَبِّئُهُم
بِمَا عَمِلُوا۟ يَوْمَ ٱلْقِيَٰمَةِ إِنَّ ٱللَّهَ بِكُلِّ شَيْءٍ عَلِيمٌ ﴿٧﴾ أَلَمْ تَرَ إِلَى ٱلَّذِينَ
نُهُوا۟ عَنِ ٱلنَّجْوَىٰ ثُمَّ يَعُودُونَ لِمَا نُهُوا۟ عَنْهُ وَيَتَنَٰجَوْنَ بِٱلْإِثْمِ
وَٱلْعُدْوَٰنِ وَمَعْصِيَتِ ٱلرَّسُولِ وَإِذَا جَآءُوكَ حَيَّوْكَ بِمَا لَمْ يُحَيِّكَ
بِهِ ٱللَّهُ وَيَقُولُونَ فِيٓ أَنفُسِهِمْ لَوْلَا يُعَذِّبُنَا ٱللَّهُ بِمَا نَقُولُ حَسْبُهُمْ
جَهَنَّمُ يَصْلَوْنَهَا فَبِئْسَ ٱلْمَصِيرُ ﴿٨﴾ يَٰٓأَيُّهَا ٱلَّذِينَ ءَامَنُوٓا۟ إِذَا
تَنَٰجَيْتُمْ فَلَا تَتَنَٰجَوْا۟ بِٱلْإِثْمِ وَٱلْعُدْوَٰنِ وَمَعْصِيَتِ ٱلرَّسُولِ وَتَنَٰجَوْا۟
بِٱلْبِرِّ وَٱلتَّقْوَىٰ وَٱتَّقُوا۟ ٱللَّهَ ٱلَّذِيٓ إِلَيْهِ تُحْشَرُونَ ﴿٩﴾ إِنَّمَا ٱلنَّجْوَىٰ
مِنَ ٱلشَّيْطَٰنِ لِيَحْزُنَ ٱلَّذِينَ ءَامَنُوا۟ وَلَيْسَ بِضَآرِّهِمْ شَيْـًٔا
إِلَّا بِإِذْنِ ٱللَّهِ وَعَلَى ٱللَّهِ فَلْيَتَوَكَّلِ ٱلْمُؤْمِنُونَ ﴿١٠﴾ يَٰٓأَيُّهَا ٱلَّذِينَ
ءَامَنُوٓا۟ إِذَا قِيلَ لَكُمْ تَفَسَّحُوا۟ فِي ٱلْمَجَٰلِسِ فَٱفْسَحُوا۟ يَفْسَحِ
ٱللَّهُ لَكُمْ وَإِذَا قِيلَ ٱنشُزُوا۟ فَٱنشُزُوا۟ يَرْفَعِ ٱللَّهُ ٱلَّذِينَ ءَامَنُوا۟
مِنكُمْ وَٱلَّذِينَ أُوتُوا۟ ٱلْعِلْمَ دَرَجَٰتٍ وَٱللَّهُ بِمَا تَعْمَلُونَ خَبِيرٌ ﴿١١﴾

kuzindikira Kwake pamalo alionse angakhale. Palibe chinthu chawo chomwe chingabisike kwa Iye. Kenako Allah Taalaa adzawafotokozera Tsiku Lakiyama zomwe adachita zabwino kapena zoipa, ndikuwalipira nazo. Ndithudi Allah ndiwodziwa chinthu chilichonse.]

8 Kodi siudaone amene aletsedwa kunong'onezana zoipa pakati pawo, kenaka akubwereza zimene adaletsedwa? Akunong'onezana za machimo, mtopola ndi kunyoza Mtumiki (SAW). Akakudzera akukulonjera (ndi malonje achinyengo) amene Allah sadakulonjerepo nawo ndipo akunena m'mitima mwawo: "Kodi n'chifukwa chiyani Allah sakutilanga ndi mawu tikunenawa (ngatidi iyeyu ndi Mtumiki (SAW) wa Allah?" Jahena ikuwakwanira adzailowa. Ndip taonani kuipa malo (awo) wobwerera.

[Kodi iwe Mtumiki (SAW) siukuwaona Ayuda amene adaletsedwa nkhani za mseri zomwe zingadzetse chikaiko m'mitima ya anthu okhulupirira kenako nkumabwerera ku zomwe adaletsedwazo, ndipo iwo nkumayankhula mwakabisibisi omwe ali machimo,mtopola ndi kusemphana ndi lamulo la Mtumiki (SAW)? Ndipo akakudzera iwe Mtumiki (SAW) Ayuda amenewa pa chinthu china chake mwazochitika, akumakulonjera ndi malonje osati amene Allah adakuikira kuti akhale malonje. Akumanena kuti: "Assaam alaika" kutanthauza kuti imfa ikhale pa iwe. Ndipo iwo akumayankhula pakati pawo kuti: "Bwanji Allah sakutilanga ndi zomwe tikuyankhula kwa Muhammad ngatidi iyeyu ali Mtumiki (SAW) wa choonadi?" Jahena yomwe akailowe idzawakwanira ndipo akasautsidwa ndi kutentha kwake, taonani kuipa malo wobwererawa.]

9 E, inu amene mwakhulupirira mwa Allah ndi Mtumiki Wake (SAW)! Ngati munganong'onezane, musamanong'onezane za machimo ndi mtopola ndi kunyoza Mtumiki (SAW). Koma nong'nezanani za kulungama ndi kuopa Allah potsatira malamulo, ndipo muopeni Allah,, kwa Iye ndi kumene mudzasonkhanitsidwe (ndi kuweruzidwa).

[E, inu amene mudavomereza Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndikugwiritsa ntchito malamulo Ake! Ngati mutayankhulana pakati panu mwachinsinsi musamayankhulane zinthu zomwe mkati mwake muli mawu a machimo kapena muli mtopola wochitira anzanu kapena kusemphana ndi lamulo la Mtumiki (SAW), m'malo mwake yankhulanani zinthu zomwe muli zabwino, zomvera ndi zochitirana ubwino. Ndipo muopeni Allah pakutsatira kwanu malamulo Ake ndikupewa kwanu zomwe adaletsa. Popeza kwa Iye Yekhayo ndiko kobwerera kwanu ndi ntchito zanu zonse, komanso zoyankhula zanu zomwe wakusungirani, ndipo adzakulipirani nazo.]

10 Ndithu, manong'onong'o oipa amachokera kwa satana, kuti adandaulitse amene akhulupirira, koma sangawapweteke nawo chili chonse kupatula atafuna Allah ndipo okhulupirira atsamire kwa Allah, yekha (asalabadire zonong'onezana zawo).

[Ndithu nkhani zakabisibisi zili za machimo, mtopola ndi manong'onong'o a satana, iye ndi amene amawakongoletsa ndikuwasenza kuti alowetse madandaulo mu mitima ya anthu okhulupirira. Izi sikuti ndizoti zikhoza kusautsa anthu okhulupirira kanthu kalikonse ayi kupatula mu chifuniro cha Allah Taalaa, ndipo kwa Allah yekhayo, atsamire anthu okhulupirira.]

11 E, inu amene mwakhulupirira mwa Allah ndi Mtumiki Wake (SAW)! Kukapemphedwa kwa inu kuti perekani malo pabwalo (pokhala); perekani malowo (kuti anzanu apeze pokhala, mukatero) Allah akuphanulirani (chifundo Chake pano pa dziko ndi kumwamba). Ndipo

يَٰٓأَيُّهَا ٱلَّذِينَ ءَامَنُوٓاْ إِذَا نَٰجَيۡتُمُ ٱلرَّسُولَ فَقَدِّمُواْ بَيۡنَ يَدَيۡ نَجۡوَىٰكُمۡ
صَدَقَةٗۚ ذَٰلِكَ خَيۡرٞ لَّكُمۡ وَأَطۡهَرُۚ فَإِن لَّمۡ تَجِدُواْ فَإِنَّ ٱللَّهَ غَفُورٞ رَّحِيمٌ
﴿١٢﴾ ءَأَشۡفَقۡتُمۡ أَن تُقَدِّمُواْ بَيۡنَ يَدَيۡ نَجۡوَىٰكُمۡ صَدَقَٰتٖۚ فَإِذۡ لَمۡ تَفۡعَلُواْ
وَتَابَ ٱللَّهُ عَلَيۡكُمۡ فَأَقِيمُواْ ٱلصَّلَوٰةَ وَءَاتُواْ ٱلزَّكَوٰةَ وَأَطِيعُواْ ٱللَّهَ
وَرَسُولَهُۥۚ وَٱللَّهُ خَبِيرُۢ بِمَا تَعۡمَلُونَ ﴿١٣﴾ ۞ أَلَمۡ تَرَ إِلَى ٱلَّذِينَ تَوَلَّوۡاْ قَوۡمًا
غَضِبَ ٱللَّهُ عَلَيۡهِم مَّا هُم مِّنكُمۡ وَلَا مِنۡهُمۡ وَيَحۡلِفُونَ عَلَى ٱلۡكَذِبِ
وَهُمۡ يَعۡلَمُونَ ﴿١٤﴾ أَعَدَّ ٱللَّهُ لَهُمۡ عَذَابٗا شَدِيدًاۖ إِنَّهُمۡ سَآءَ مَا كَانُواْ
يَعۡمَلُونَ ﴿١٥﴾ ٱتَّخَذُوٓاْ أَيۡمَٰنَهُمۡ جُنَّةٗ فَصَدُّواْ عَن سَبِيلِ ٱللَّهِ فَلَهُمۡ
عَذَابٞ مُّهِينٞ ﴿١٦﴾ لَّن تُغۡنِيَ عَنۡهُمۡ أَمۡوَٰلُهُمۡ وَلَآ أَوۡلَٰدُهُم مِّنَ ٱللَّهِ
شَيۡـًٔاۚ أُوْلَٰٓئِكَ أَصۡحَٰبُ ٱلنَّارِۖ هُمۡ فِيهَا خَٰلِدُونَ ﴿١٧﴾ يَوۡمَ يَبۡعَثُهُمُ
ٱللَّهُ جَمِيعٗا فَيَحۡلِفُونَ لَهُۥ كَمَا يَحۡلِفُونَ لَكُمۡۖ وَيَحۡسَبُونَ أَنَّهُمۡ عَلَىٰ شَيۡءٍۚ أَلَآ
إِنَّهُمۡ هُمُ ٱلۡكَٰذِبُونَ ﴿١٨﴾ ٱسۡتَحۡوَذَ عَلَيۡهِمُ ٱلشَّيۡطَٰنُ فَأَنسَىٰهُمۡ ذِكۡرَ
ٱللَّهِۚ أُوْلَٰٓئِكَ حِزۡبُ ٱلشَّيۡطَٰنِۚ أَلَآ إِنَّ حِزۡبَ ٱلشَّيۡطَٰنِ هُمُ ٱلۡخَٰسِرُونَ
﴿١٩﴾ إِنَّ ٱلَّذِينَ يُحَآدُّونَ ٱللَّهَ وَرَسُولَهُۥٓ أُوْلَٰٓئِكَ فِي ٱلۡأَذَلِّينَ ﴿٢٠﴾
كَتَبَ ٱللَّهُ لَأَغۡلِبَنَّ أَنَا۠ وَرُسُلِيٓۚ إِنَّ ٱللَّهَ قَوِيٌّ عَزِيزٞ ﴿٢١﴾

kukanenedwa kuti imiririrani, muimirire (musanyozere, apatseni ena malo), Allah awakwezera (ulemerero) mwa inu amene akhulupirira ndi amene apatsidwa nzeru. Ndipo Allah akudziwa bwino zimene mukuchita.

[E, inu amene mudam'vomereza Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndi kugwiritsa ntchito malamulo Ake! Ngati mutapemphedwa kuti afutukireni anzanu malo okhala, futukani, Allah akutambasulirani pano pa dziko lapansi komanso Tsiku Lomaliza. Ndipo mukapemphedwa inu anthu okhuluipirira kuti muimirire kuchoka pamalo panu pachifukwa mu zifukwa zina zomwe muli zabwino kwa inu, ndiye imiririrani, Allah atukula ulemerero wa anthu okhulupirira odziyeretsa mwa inu, komanso atukula ulemerero wa anthu ozindikira ulemerero wambiri mu malipiro komanso chiyanjo. Ndipo Allah Taalaa ndi wozindikira za ntchito zanu zonse, palibe kobisika kalikonse mu zimenezo ndipo Iye adzakulipirani nazo. Mu ayat imeneyi muli kufotokozera za ulemerero wa anthu ozindikira, ubwino wawo ndi kutukuka kwa ulemerero wawo.]

(12) E, inu amene mwakhulupirira! Mukafuna kuyankhula ndi Mtumiki (SAW) mwa mseri, tsogozani pa zoyankhula zanuzo sadaka; kutero ndibwino kwa inu ndiponso ndichoyeretsa (mitima yanu) koma ngati simudapeze (sadakayo) ndithu Allah Ngokhululuka, Ngwachisoni.

[E, inu amene mudamvomera Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndikugwiritsa ntchito malamulo Ake! Ngati mutafuna kumuyankhula Mtumiki (SAW) mwamseri, tsogozani musadatero kupereka sadaka kwa osowa, zimenezo ndi zabwino kwa inu chifukwa choti muli malipiro komanso chiyero cha mitima yanu ku machimo. Ngati simudapeze choperekera sadakacho, ndiye kuti palibe vuto kwa inu. Ndithu Allah Ngokhululukira akapolo Ake okhulupirira, komanso amawachitira chisoni.]

(13) Kodi mwaopa kutsogoza sadaka pakunena naye (Mtumiki (SAW)? Ngati simudachite zimenezi, Allah wakukhululukirani, choncho pempherani swalaat moyenerera ndipo perekani Zakaat komanso mverani Allah pamodzi ndi Mtumiki Wake (SAW). Ndipo Allah akudziwa zonse zimene mukuchita.

[Kodi mukuopa kusauka ngati mutati mutsogogoze sadaka musadayankhulane ndi Mtumiki (SAW) wa Allah mwa mseri? Ngati simuchita zomwe mwalamulidwazo ndiye kuti Allah wakukhululukirani ndipo wakulolezani kuti musamatero, choncho kakamirani ndipo pitirizani popemphera Swalaat mwadongosolo, kupereka Zakaat ndikumvera Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) mu chilichonse chimene mwalamulidwa nacho. Ndipo Allah Subhaanahu ndi wozindikira za ntchito zanu zonse ndipo akakulipirani nazo.]

(14) Kodi siukuwaona awo amene achita chibwenzi ndi anthu amene Allah wawakwiyira; iwo Sali mwa inu ndiponso Sali mwa iwo. Ndipo akulumbira zabodza uku akudziwa (kuti limeneli ndi bodza).

[Kodi sukuwaona achiphamasowa amene awachita Ayuda kukhala abwenzi ndikuyanjana nawo? Kunena zoona achiphamaso sali m'gulu la Asilamu ngakhalenso gulu la Ayuda. Ndipo akumalumbira zabodza kuti iwo ndi Asilamu kumachita kuti akudziwa kuti iwowo akunama pa zomwe akulumbirazo.]

(15) Allah wawakonzera chilango chaukali, ndithudi zimene amachita n'zoipa.

[Allah wawakonzera achiphamaso amenewa chilango chopweteka kwambiri. Ndithudi n'zoipa zimene amakhala akuchita za uchipha maso ndikulumbira zabodza.]

(16) Kulumbira kwawo adakuchita kukhala

chodzitetezera (iwo, ana awo ndi chuma chawo); choncho adatsekereza (anthu) ku njira ya Allah, ndipo chilango choyalutsa chili pa iwo.
[Achichita achiphamaso chikhulupiriro chawo chabodzacho kukhala chodzitetezera chawo kuti asaphedwe chifukwa cha kukanira kwawoko, ndinso kuletsa Asilamu zowathira nkhondo, ndikutenga chuma chawo. Kwa chifukwa chimenechi iwo adzitsekerezera eni akewo komanso ena ku njira ya Allah yomwe ndi Chisilamu. Ndiye ali nacho chilango choyalutsa ku jahena chifukwa chodzikweza kwawo, kuleka kumukhulupirira Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndikutsekereza kwawo ku njira Yake.]
17 Chuma chawo ngakhale ana awo sizidzawathandiza konse ku chilango cha Allah. Iwowo ndi anthu a ku moto. M'menemo iwo adzakhala muyaya.
[Sichidzateteza achiphamaso chuma chawo ngakhale ana awo ku chilango cha Allah kanthu kalikonse. Iwowo ndi ndi anthu a ku moto womwe akaulowe nakakhalamo muyaya osakatulukamo. Malipiro amenewa akukhudza aliyense amene akutsekereza ku chipembedzo cha Allah ndi liwu lake kapena zochita zake.]
18 (Alikumbukire) tsiku limene Allah adzaukitse onse (ku imfa), ndipo onse adzayamba kulumbira kwa Iye (zabodza) monga akulumbira (zabodza) kwa inu. Akuganiza kuti apezapo kanthu (pakulumbira kwawo); dziwani, ndithudi iwo ndi abodza.
[Tsiku Lachiweruzo Allah adzawaukitsa achiphamaso onse kuchokera m'manda awo kukhalanso amoyo, ndipo azidzalumbira kwa Iye kuti ndithu iwo adali okhulupirira monga m'mene ankachitira pokulumbirirani inu amene mudakhulupirira pa dziko lapansi. Ndipo adzikatsimikiza kuti zimenezo zikawathandizanso kwa Allah monga m'mene zinkawathandizira pa dziko lapansi kwa anthu okhulupirira. Dziwani kuti iwowo ndi opyoza malire pa bodza pa mulingo umene sadaufikeko ena alionse.]
19 Satana wawapambana ndipo wawaiwalitsa kukumbukira Allah. Iwowa ndi a chipani cha satana. Dziwani kuti chipani cha satana n'chotaika (choonongeka). [Satana wawapambana iwowo ndipo wawagonjetsa kufikira kuti asiya malamulo a Allah ndi kugwira ntchito pomumvera Iye. Iwowo ndi a gulu la satana komanso omutsatira ake. Dziwani kuti ndithudi gulu la satana ndi lotaika pa dziko lapansi komanso Tsiku Lomaliza.]
20 Ndithudi, amene akutsutsana ndi Allah ndi Mtumiki Wake (SAW),iwowo adzakhala m'gulu la onyozeka. [Ndithu anthu amene akutsutsa lamulo la Allah ndi Mtumiki Wake (SAW), iwowo ali m'gulu la anthu oyalutsidwa komanso ogonjetsedwa pa dziko lino lapansi komanso Tsiku Lomaliza.]
21 Allah adalamula (kuti): "Ndipambana Ine ndi Aneneri Anga". Ndithu Allah ndiwanyonga zokwana, wopambana (sagonjetsedwa ndi wina aliyense). Allah adalemba mu kaundula wamkulu (Allahuhil Mahfuuz) ndipo adalamula kuti kugonjetsa nkwa Iye, buku Lake, Atumiki Ake ndi akapolo Ake okhulupirira. Ndithu Allah Subhaanahu Ngwamphamvu palibe chimene chingamulephere Ngopambana pa zolengedwa Zake zonse.
22 Siupeza anthu okhulupirira mwa Allah ndi Tsiku Lomaliza akuwakonda amene akumuda Allah ndi Mtumiki Wake ngakhale atakhala atate awo, ana awo, abale awo ndi akumtundu kwawo; kwa iwo Allah wazika chikhulupiriro (champhamvu) m'mitima mwawo, ndipo walimbikitsa ndi mphamvu zochokera kwa Iye. Ndipo adzawalowetsa m'minda yomwe pansi pake pakuyenda mitsinje; adzakhala m'menemo muyaya. Allah adzakondwera nawo ndipo (iwonso) adzakondwera Naye, iwowa ndi chipani cha Allah. Dziwani kuti chipani cha Allah ndi chopambana.
[Iwe Mtumiki (SAW) siupeza anthu amene amamuvomereza Allah, Tsiku Lomaliza ndi kumagwiritsa ntchito zimene Allah adawalamula, akukonda komanso kupalana ubwenzi ndi munthu amene akumuda Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) nkumatsutsana ndi malamulo awo. Awa ngakhalae atakhala atate awo, ana awo,azichimwene ndi alongo awo ngakhalenso abale awo, iwowa amakondana ndi kupalana ubwenzi chifukwa cha Allah komanso amadana chifukwa cha Iye, Allah walimbikitsa m'mitima yawo chikhulupiriro ndipo awalimbikitsa ndi chigonjetso chochokera kwa Iye ndi chithandizo Chake pa adani awo pano pa dziko lapansi ndipo akawalowetsa Tsiku Lomaliza ku jannat pansi pa mitengo yake pakuyenda mitsinje. Akakhala m'menemo nyengo yosadukiza. Allah adzawapatsa chiyanjo Chake kotero sadzawapsera mtima ndipo iwo adzakondwera ndi Mbuye Wawo pa zomwe adzawapatsa maulemerero apamwamba. Iwowo ndi gulu la Allah komanso abwenzi Ake ndipo iwowo ndi opambana ndi chisangalalo cha pa dziko lapansi komanso Tsiku Lomaliza]

# (59) SURATUL HASHR

لَّا تَجِدُ قَوْمًا يُؤْمِنُونَ بِٱللَّهِ وَٱلْيَوْمِ ٱلْـَٔاخِرِ يُوَآدُّونَ مَنْ
حَآدَّ ٱللَّهَ وَرَسُولَهُۥ وَلَوْ كَانُوٓا۟ ءَابَآءَهُمْ أَوْ أَبْنَآءَهُمْ
أَوْ إِخْوَٰنَهُمْ أَوْ عَشِيرَتَهُمْ ۚ أُو۟لَـٰٓئِكَ كَتَبَ فِى قُلُوبِهِمُ
ٱلْإِيمَـٰنَ وَأَيَّدَهُم بِرُوحٍ مِّنْهُ ۖ وَيُدْخِلُهُمْ جَنَّـٰتٍ تَجْرِى
مِن تَحْتِهَا ٱلْأَنْهَـٰرُ خَـٰلِدِينَ فِيهَا ۚ رَضِىَ ٱللَّهُ عَنْهُمْ وَرَضُوا۟
عَنْهُ ۚ أُو۟لَـٰٓئِكَ حِزْبُ ٱللَّهِ ۚ أَلَآ إِنَّ حِزْبَ ٱللَّهِ هُمُ ٱلْمُفْلِحُونَ ٢٢

آياتها ٢٤ — سُورَةُ الحَشْرِ — ترتيبها ٥٩

بِسْمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحْمَـٰنِ ٱلرَّحِيمِ

سَبَّحَ لِلَّهِ مَا فِى ٱلسَّمَـٰوَٰتِ وَمَا فِى ٱلْأَرْضِ ۖ وَهُوَ ٱلْعَزِيزُ ٱلْحَكِيمُ
١ هُوَ ٱلَّذِىٓ أَخْرَجَ ٱلَّذِينَ كَفَرُوا۟ مِنْ أَهْلِ ٱلْكِتَـٰبِ مِن دِيَـٰرِهِمْ
لِأَوَّلِ ٱلْحَشْرِ ۚ مَا ظَنَنتُمْ أَن يَخْرُجُوا۟ ۖ وَظَنُّوٓا۟ أَنَّهُم مَّانِعَتُهُمْ
حُصُونُهُم مِّنَ ٱللَّهِ فَأَتَىٰهُمُ ٱللَّهُ مِنْ حَيْثُ لَمْ يَحْتَسِبُوا۟ ۖ وَقَذَفَ
فِى قُلُوبِهِمُ ٱلرُّعْبَ ۚ يُخْرِبُونَ بُيُوتَهُم بِأَيْدِيهِمْ وَأَيْدِى ٱلْمُؤْمِنِينَ
فَٱعْتَبِرُوا۟ يَـٰٓأُو۟لِى ٱلْأَبْصَـٰرِ ٢ وَلَوْلَآ أَن كَتَبَ ٱللَّهُ عَلَيْهِمُ
ٱلْجَلَآءَ لَعَذَّبَهُمْ فِى ٱلدُّنْيَا ۖ وَلَهُمْ فِى ٱلْـَٔاخِرَةِ عَذَابُ ٱلنَّارِ ٣

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Zonse za m'mwamba ndi za pansi zimalemekeza Allah (ndikumuteteza kukhalidwe losayenera ndi ulemerero Wake). Ndipo Iye Ngopambana, (salephera kanthu) Ngwaluntha (m'kakonzedwe Kake ndi zochita Zake.

[Chinthu chili chonse chomwe chili kumwamba komanso pa dziko lapansi, chayeretsa Allah molingana ndi ulemerero Wake. Ngopambana Amene sagonjetsedwa, Wanzeru zakuya pakakonzedwe Kake ka zinthu, kalinganizidwe Kake, mu zochita Zake ndi kaikidwe Kake kamalamulo, amaika zinthu zonse m'chimache.]

2 Iye ndi Amene adatulutsa osakhulupirira ena mwa anthu a mabuku m'nyumba zawo nkusamuka koyamba (pa chilumba cha Arabu). Simunkaganizira kuti angatuluke (m'nyumba zawozo). Ndipo iwo amaganiza kuti malinga awo awateteza ku (chilango cha) Allah. Koma Allah adawalanga kupyolera m'mene samayembekezera, ndipo adathira mantha oopsa m'mitima mwawo (potumiza Mtumiki Wake (SAW) kwa iwo), adagumula nyumba zawo ndi manja awo ndiponso manja a okhulupirira. Talingalirani (zimenezi) E, inu eni nzeru!

[Iye Subhaanahu ndi Amene adawatulutsa anthu amene adakanira uneneri wa Muhammad (SAW) mu gulu la eni buku amene ali a Ayuda a Bani AlNadhiir kuchokera m'nyumba zawo zimene zidayandikana ndi Asilamu m'mphepete mwa mzinda wa Madina. Ndipo kumeneku kunali kutulutsidwa koyamba kwa iwo kuchoka m'chirumba cha Arab kupita ku Shaam (Syria). Simunkaganiza inu Asilamu kuti iwowo angatuluke m'nyumba zawo ali oyalutsidwa ndi apansi chifukwa champhamvu zawo pa nkhondo ndi mphamvu za chitetezo chawo. Ayuda ankaganiza kuti malinga awo awateteza ku mphamvu za Allah ndipo palibe amene angawathe iwo. Choncho Allah adawabwerera kuchokera komwe samaganizira mpang'ono pomwe m'maganizo mwawo. Ndipo adaika m'mitima mwawo mantha ndi kunjenjemera kwakukulu. Amagumula nyumba zawo ndi manja awo komanso, manja a anthu okhulupirira. Kotero ganizirani mozama e, inu eni maso olungama ndi nzeru zakuya.]

3 Ndipo kukadapanda kuti Allah adawalembera (pachiyambi) kusamuka (m'nyumba zawo), akadawalanga pa dziko la pansi pompano. Koma chilango cha moto chili pa iwo Tsiku Lomaliza. [Chipanda Allah kuwalembera zoti atuluke m'nyumba zawo ndi chigamulo Chake, bwenzi atawalanga pa dziko la pansi pophedwa ndi kutengedwa ngati akapolo. Ndipo ali nacho chilango cha moto.]

4 Zimenezo n'chifukwa chakuti iwo adamuda Allah ndi Mtumiki (SAW) Wake, (chidani chopyola muyeso); ndipo amene akumuda Allah (sangapulumuke ku chilango Chake). Ndithu Allah ndi Wolanga mwaukali.

[Zomwe zidawapeza Ayuda pa dziko lapansi ndi zomwe zikuwayembekekezera Tsiku Lomaliza, ndi chifukwa choti iwowo adatsutsana ndi lamulo la Allah komanso Mtumiki Wake (SAW) kutsutsana kwakukulu ndipo adawathira nkhondo. Amene atsutsane ndi Allah komanso Mtumiki Wake (SAW), ndithu Allah ndi Wopereka chilango cholapitsa kwa iwo.]

5 Sim'dadule mtengo uliwonse wa zipatso za kanjedza, (inu Asilamu), kapena kuwusiya uli chiimire ndi thundu lake koma ndi chifuniro cha Allah, ndikuti awayalutse otuluka m'malamulo Ake. [Inu anthu okhulupirira, simunadule mitengo ya kanjedza kapena kuisiya chiimire pa maphata ake popanda kuichita kanthu, zonsezo zidachitika ndi chilolezo cha Allah ndi lamulo Lake.

ذَٰلِكَ بِأَنَّهُمْ شَآقُّوا۟ ٱللَّهَ وَرَسُولَهُۥ ۖ وَمَن يُشَآقِّ ٱللَّهَ فَإِنَّ ٱللَّهَ شَدِيدُ
ٱلْعِقَابِ ﴿٤﴾ مَا قَطَعْتُم مِّن لِّينَةٍ أَوْ تَرَكْتُمُوهَا قَآئِمَةً
عَلَىٰٓ أُصُولِهَا فَبِإِذْنِ ٱللَّهِ وَلِيُخْزِىَ ٱلْفَٰسِقِينَ ﴿٥﴾ وَمَآ أَفَآءَ ٱللَّهُ
عَلَىٰ رَسُولِهِۦ مِنْهُمْ فَمَآ أَوْجَفْتُمْ عَلَيْهِ مِنْ خَيْلٍ وَلَا رِكَابٍ
وَلَٰكِنَّ ٱللَّهَ يُسَلِّطُ رُسُلَهُۥ عَلَىٰ مَن يَشَآءُ ۚ وَٱللَّهُ عَلَىٰ كُلِّ شَىْءٍ
قَدِيرٌ ﴿٦﴾ مَّآ أَفَآءَ ٱللَّهُ عَلَىٰ رَسُولِهِۦ مِنْ أَهْلِ ٱلْقُرَىٰ فَلِلَّهِ وَلِلرَّسُولِ
وَلِذِى ٱلْقُرْبَىٰ وَٱلْيَتَٰمَىٰ وَٱلْمَسَٰكِينِ وَٱبْنِ ٱلسَّبِيلِ كَىْ لَا يَكُونَ
دُولَةًۢ بَيْنَ ٱلْأَغْنِيَآءِ مِنكُمْ ۚ وَمَآ ءَاتَىٰكُمُ ٱلرَّسُولُ فَخُذُوهُ وَمَا
نَهَىٰكُمْ عَنْهُ فَٱنتَهُوا۟ ۚ وَٱتَّقُوا۟ ٱللَّهَ ۖ إِنَّ ٱللَّهَ شَدِيدُ ٱلْعِقَابِ ﴿٧﴾
لِلْفُقَرَآءِ ٱلْمُهَٰجِرِينَ ٱلَّذِينَ أُخْرِجُوا۟ مِن دِيَٰرِهِمْ وَأَمْوَٰلِهِمْ
يَبْتَغُونَ فَضْلًا مِّنَ ٱللَّهِ وَرِضْوَٰنًا وَيَنصُرُونَ ٱللَّهَ وَرَسُولَهُۥٓ ۚ أُو۟لَٰٓئِكَ
هُمُ ٱلصَّٰدِقُونَ ﴿٨﴾ وَٱلَّذِينَ تَبَوَّءُو ٱلدَّارَ وَٱلْإِيمَٰنَ مِن قَبْلِهِمْ
يُحِبُّونَ مَنْ هَاجَرَ إِلَيْهِمْ وَلَا يَجِدُونَ فِى صُدُورِهِمْ حَاجَةً
مِّمَّآ أُوتُوا۟ وَيُؤْثِرُونَ عَلَىٰٓ أَنفُسِهِمْ وَلَوْ كَانَ بِهِمْ خَصَاصَةٌ ۚ
وَمَن يُوقَ شُحَّ نَفْسِهِۦ فَأُو۟لَٰٓئِكَ هُمُ ٱلْمُفْلِحُونَ ﴿٩﴾

Ndikuti awayalutse ndi zimenezo anthu amene atuluka mu kumvera Iye, otsutsana ndi lamulo Lake ndi zimene waletsa, kotero Allah adakupatsani mphamvu zodula mitengo ya kanjedza yawo ndikuiotcha.]

(6) Ndipo chuma chimene wapereka Allah kwa Mtumiki Wake (SAW) chochokera kwa iwo (Bani Nadhwir), chimenecho inu simudathamangitse akavalo kapena ngamira (pakuchipeza) koma Allah amapereka mphamvu kwa atumiki Ake (zogonjetsera) amene wam'funa. Ndipo Allah ali ndi mphamvu (yochita) chilichonse.

[Ndipo zomwe Allah wazipereka kwa Mtumiki Wake (SAW) mu chuma cha Ayuda a Bani Nadhwir ndipo inu simudakwere akavalo kapena ngamira kuti muchipeze koma Allah amapatsa mphamvu atumiki Ake pogonjetsa amene Allah wawafuna mwa adani Ake, kotero nkumakalandira chuma chosachitira nkhondo. Ndipo Allah ndi Wokhoza kuchita kanthu kalikonse, palibe chomulepheretsa.]

(7) Chuma chimene Allah wachipereka kwa Mtumiki Wake (SAW) cha anthu am'midzi (yapafupi ndi mzinda wa Madina) chimenecho ncha Allah, ndi Mtumiki (SAW), achibale a Mtumiki (SAW), amasiye, masikini ndiponso apaulendo; kuti chisakhale chongozungulira pakati pa olemera mwa inu. Ndipo chimene wakupatsani Mtumiki (SAW), chilandireni ndipo chimene wakuletsani chisiyeni. Muopeni Allah (potsatira malamulo Ake) ndithu Allah Ngwaukali polanga.

[Chomwe Allah wachipereka kwa Mtumiki Wake (SAW) mu chuma cha a mushrikina a m'midzi yosiyanasiyana popanda kukwerera akavalo kapena ngamira chimencho n'cha Allah ndi Mtumiki Wake (SAW), chiperekedwe ku zinthu zokomera Asilamu onse, kwa abale a Mtumiki wa Allah (SAW), amasiye - amenewo ndi ana osauka amene makolo awo adamwalira -, komanso kwa osowa, amenewo ndi anthu amene asowekera thandizo komanso kusauka; kudzanso kwa wa paulendo yemwe ndi mlendo wa paulendo amene zamuthera zithandizo zake ndipo chuma chake chamudukira. Zikhale dero kuti chuma chisamakhale umwini wake wongozungulira pakati pa olemera okhawo nkumamanidwa anthu osauka ndi osowa. Ndipo chomwe Mtumiki (SAW) wakupatsani mu gawo la chuma kapena wakupatsani lamumlo lina lake m'malamulo a Allah, inu chitengeni ndipo chimene wakuletsani kuchitenga kapena kuchichita chisiyeni. Ndipo muopeni Allah potsatira malamulo Ake ndi kusiya zomwe waletsa. Ndithu Allah Ngolanga molapitsa kwa munthu amene wamulakwira ndikutsutsana ndi lamulo Lake ndi zoletsedwa Zake. Ayat imeneyi ndi tsinde lachikakamizo chogwiritsira ncthito sunnat za Mtumiki (SAW) zomwe ndi mawu ake, ntchito zake ndi kuvomereza kwake kwa zinthu zimene zimachitika iye ali pomwepo.]

(8) (Choncho) chiperekedwe (chumacho) kwa osauka osamuka omwe adatulutsidwa m'nyumba zawo (kusiya) chuma chawo chifukwa chofuna zabwino za Allah ndi chikondi (Chake) ndi kupulumutsa chipembedzo cha Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) (potumikira matupi awo ndi chuma chawo); iwowa ndi (Asilamu) oona.

[M'menemo ndimomwe apatsidwire chuma chimene Allah wachipereka kwa Mtumiki Wake (SAW), anthu osauka, osamuka amene makafiri a pa Makka adawapanikiza mpaka potuluka ndikusiya nyumba zawo ndi chuma chawo uku akufuna kuchokera kwa Allah kuti awapatse rizq pano pa dziko lapansi komanso chiyanjo (Chake) pa Tsiku Lomaliza ndipo nkumateteza chipembedzo cha Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) pochita jihaad mu njira ya Allah, iwowa ndi oona mtima amene ntchito zawo zavomereza mawu awo.]

وَٱلَّذِينَ جَآءُو مِنۢ بَعۡدِهِمۡ يَقُولُونَ رَبَّنَا ٱغۡفِرۡ لَنَا
وَلِإِخۡوَٰنِنَا ٱلَّذِينَ سَبَقُونَا بِٱلۡإِيمَٰنِ وَلَا تَجۡعَلۡ فِي قُلُوبِنَا
غِلّٗا لِّلَّذِينَ ءَامَنُواْ رَبَّنَآ إِنَّكَ رَءُوفٞ رَّحِيمٌ ١٠ أَلَمۡ تَرَ إِلَى
ٱلَّذِينَ نَافَقُواْ يَقُولُونَ لِإِخۡوَٰنِهِمُ ٱلَّذِينَ كَفَرُواْ مِنۡ أَهۡلِ
ٱلۡكِتَٰبِ لَئِنۡ أُخۡرِجۡتُمۡ لَنَخۡرُجَنَّ مَعَكُمۡ وَلَا نُطِيعُ فِيكُمۡ
أَحَدًا أَبَدٗا وَإِن قُوتِلۡتُمۡ لَنَنصُرَنَّكُمۡ وَٱللَّهُ يَشۡهَدُ إِنَّهُمۡ لَكَٰذِبُونَ
١١ لَئِنۡ أُخۡرِجُواْ لَا يَخۡرُجُونَ مَعَهُمۡ وَلَئِن قُوتِلُواْ لَا يَنصُرُونَهُمۡ
وَلَئِن نَّصَرُوهُمۡ لَيُوَلُّنَّ ٱلۡأَدۡبَٰرَ ثُمَّ لَا يُنصَرُونَ ١٢
لَأَنتُمۡ أَشَدُّ رَهۡبَةٗ فِي صُدُورِهِم مِّنَ ٱللَّهِۚ ذَٰلِكَ بِأَنَّهُمۡ قَوۡمٞ
لَّا يَفۡقَهُونَ ١٣ لَا يُقَٰتِلُونَكُمۡ جَمِيعًا إِلَّا فِي قُرٗى
مُّحَصَّنَةٍ أَوۡ مِن وَرَآءِ جُدُرِۭۚ بَأۡسُهُم بَيۡنَهُمۡ شَدِيدٞۚ تَحۡسَبُهُمۡ
جَمِيعٗا وَقُلُوبُهُمۡ شَتَّىٰۚ ذَٰلِكَ بِأَنَّهُمۡ قَوۡمٞ لَّا يَعۡقِلُونَ ١٤
كَمَثَلِ ٱلَّذِينَ مِن قَبۡلِهِمۡ قَرِيبٗاۖ ذَاقُواْ وَبَالَ أَمۡرِهِمۡ وَلَهُمۡ عَذَابٌ
أَلِيمٞ ١٥ كَمَثَلِ ٱلشَّيۡطَٰنِ إِذۡ قَالَ لِلۡإِنسَٰنِ ٱكۡفُرۡ فَلَمَّا كَفَرَ
قَالَ إِنِّي بَرِيٓءٞ مِّنكَ إِنِّيٓ أَخَافُ ٱللَّهَ رَبَّ ٱلۡعَٰلَمِينَ ١٦

(9) Koma amene adakhala kale mu mzinda uwu (wa Madina) ndi kukhulupirira akukonda amene adasamukira kwa iwo. Ndipo sakupeza vuto m'mitima mwawo pazimene anzawo apatsidwa, ndipo akutsogoza zofuna za anzawo pa za iwo ngakhale iwo akuzifunitsitsa. Amene atetezedwa (ndi Allah) ku umbombo wa mitima yawo, amenewo ndiwo opambana.

[Ndipo anthu amene adakhala kale mu mzinda wa Madina nakhulupirira kusadachitike msamuko wa Mamuhaajirina – amenewo ndi ansaar (nzika za Madina)- amawakonda anthu osamuka ndikumagawana nawo chuma chawo, ndipo sapeza m'mitima mwawo nsanje yochitira iwowa mu zomwe adapatsidwa mu chuma chimene Mtumiki (SAW) adapatsidwa mopanda kuchitira nkhondo ndi zina, ndipo iwo akumatsogoza anthu osamuka ndi omwe ali osowa pa iwo ; zimakhala dero angakhale iwo eni akewo ali ndi vuto ndikusowekera. Munthu amene wapulumuka ku umbombo ndi kumana ena mu chuma, ndiye kuti iwowo ndiwo opambana amene akapeze zofuna zawo.]

(10) Ndipo (okhulupirira) amene adadza pambuyo (pa Amuhaajirina ndi Ansaari) akunena kuti: "Mbuye wathu tikhululukireni ndi abale athu amene adatitsogolera pa chikhulupiriro, ndipo musaike m'mitima mwathu njiru ndi chidani kwa amene adakhulupirira. O, Mbuye wathu! Inu ndinu Wodekha, Wachisoni". [Ndipo anthu amene abwera a mu gulu la okhulupirira pambuyo pa Ansari ndi Mamuhaajirina oyambirira amanena kuti : "Mbuye wathu! Tikhululukireni ife machimo athu, komanso akhululukireni abale athu mu chipembedzo amene adatitsogolera ife ndi chikhulupiriro, ndipo musake m'mitima mwathu kaduka ndikuipidwa, kwa aliyense mwa anthu a chikhulupiriro. Mbuye wathu! Ndithudi inu ndi Wodekha ndi akapolo Anu, Wachisoni ndi iwo." Mu Ayat imeneyi muli umboni wosonyeza kuti nkoyenera kwa Msilamu kuti aziwatchula amene adamutsogolera ndi zabwino ndikumawafunira chiyanjo cha Allah.]

(11) Kodi wawona achinyengo amene akunena kwa anzawo amene sadakhulupirire pakati pa anthu a Mabuku: "pali Allah, ngati (mukakamizidwa) kutuluka mu mzinda wa Madina, tidzatuluka nanu pamodzi ndipo sitingamvere aliyense za inu mpaka muyaya; ngati mutamenyedwa nkhondo (ndi Asilamu) tidzakuthandizani. Koma Allah akuikira umboni kuti iwo ndi onama (pazimene alonjeza) [Kodi siudawaone achiphamaso akunena kwa abale awo mu ukafiri m'gulu la Ayuda a Bani Nadhwiri: "Ngati Muhammad (SAW) ndi anthu amene ali naye atakutulutsani mu nyumba zanu, ndithu ife tidzatuluka nanu, ndipo sitidzamvera wina aliyense za inu mpaka muyaya, zoti tikulekeni osakuthandizani ndikusiya kutluka nanu limodzi, ndipo ngati mutathiridwa nkhondo, ndithudi tidzakuthandizani?" Ndipo Allah akuikira umboni kuti ndithu achiphamasowa akunama mu zomwe alonjezazi kwa Ayuda a Bani Nadhwiri.]

(12) Koma akapirikitsidwa, sangatuluke nawo limodzi; ngati atathiridwa nkhondo, sangawathandize ngati atawathandiza atembenuza misana (kuthawa) kenako sapulumutsidwa.

[Ngati Ayuda atapirikitsidwa mu mzinda wa Madina, achiphamaso sangatuluke nawo limodzi, komanso ngati atatsiridwa nkhondo, sangamenyane nawo limodzi monga adalonjezerera, ndipo adakati achitire limodzi nkhondo, mtheradi atembenuza misana yawo kuthawa mogonja, kenako Allah samawathandiza koma amawataya ndikuwayalutsa.]

(13) Ndithu inu (Asilamu) mukuopedwa kwambiri m'mitima mwawo kuposa m'mene

فَكَانَ عَٰقِبَتَهُمَآ أَنَّهُمَا فِي ٱلنَّارِ خَٰلِدَيۡنِ فِيهَاۚ وَذَٰلِكَ جَزَٰٓؤُاْ
ٱلظَّٰلِمِينَ ١٧ يَٰٓأَيُّهَا ٱلَّذِينَ ءَامَنُواْ ٱتَّقُواْ ٱللَّهَ وَلۡتَنظُرۡ
نَفۡسٞ مَّا قَدَّمَتۡ لِغَدٖۖ وَٱتَّقُواْ ٱللَّهَۚ إِنَّ ٱللَّهَ خَبِيرُۢ بِمَا تَعۡمَلُونَ
١٨ وَلَا تَكُونُواْ كَٱلَّذِينَ نَسُواْ ٱللَّهَ فَأَنسَىٰهُمۡ أَنفُسَهُمۡۚ أُوْلَٰٓئِكَ
هُمُ ٱلۡفَٰسِقُونَ ١٩ لَا يَسۡتَوِيٓ أَصۡحَٰبُ ٱلنَّارِ وَأَصۡحَٰبُ
ٱلۡجَنَّةِۚ أَصۡحَٰبُ ٱلۡجَنَّةِ هُمُ ٱلۡفَآئِزُونَ ٢٠ لَوۡ أَنزَلۡنَا هَٰذَا
ٱلۡقُرۡءَانَ عَلَىٰ جَبَلٖ لَّرَأَيۡتَهُۥ خَٰشِعٗا مُّتَصَدِّعٗا مِّنۡ خَشۡيَةِ
ٱللَّهِۚ وَتِلۡكَ ٱلۡأَمۡثَٰلُ نَضۡرِبُهَا لِلنَّاسِ لَعَلَّهُمۡ يَتَفَكَّرُونَ
٢١ هُوَ ٱللَّهُ ٱلَّذِي لَآ إِلَٰهَ إِلَّا هُوَۖ عَٰلِمُ ٱلۡغَيۡبِ وَٱلشَّهَٰدَةِۖ
هُوَ ٱلرَّحۡمَٰنُ ٱلرَّحِيمُ ٢٢ هُوَ ٱللَّهُ ٱلَّذِي لَآ إِلَٰهَ إِلَّا هُوَ
ٱلۡمَلِكُ ٱلۡقُدُّوسُ ٱلسَّلَٰمُ ٱلۡمُؤۡمِنُ ٱلۡمُهَيۡمِنُ ٱلۡعَزِيزُ
ٱلۡجَبَّارُ ٱلۡمُتَكَبِّرُۚ سُبۡحَٰنَ ٱللَّهِ عَمَّا يُشۡرِكُونَ
٢٣ هُوَ ٱللَّهُ ٱلۡخَٰلِقُ ٱلۡبَارِئُ ٱلۡمُصَوِّرُۖ لَهُ ٱلۡأَسۡمَآءُ ٱلۡحُسۡنَىٰۚ
يُسَبِّحُ لَهُۥ مَا فِي ٱلسَّمَٰوَٰتِ وَٱلۡأَرۡضِۖ وَهُوَ ٱلۡعَزِيزُ ٱلۡحَكِيمُ ٢٤

## سُورَةُ المُمۡتَحنَة

ترتيبها ٦٠ — آياتها ١٣

akumuopera Allah. Zimenezo n'chifukwa chakuti iwo ndi anthu osazindikira (chilichonse za kukhulupirira mwa Allah).

[Ndithudi mantha a achiphamaso ndikukuopani kwawo inu anthu okhulupirira ngakulu zedi m'mitima mwawo kuposa kuopa kwawo Allah chifukwa choti iwowo sazindikira ukulu wa Allah ndi kukhulupirira mwa Iye ndikutinso saopa chilango Chake.]

(14) (Ayuda) sangamenyane ndi inu ali pa gulu kupatula m'midzi yotetezedwa ndi malinga, kapena kuseri kwa zipupa, nkhondo yawo pakati pawo njaukali; ungawaganizire kuti ali limodzi pomwe mitima yawo njosiyana. Zimenezo n'chifukwa chakuti iwo ndi anthu opanda nzeru. [Ayuda ali pa gulu sangachite nanu nkhondo pamasompamaso kupatula ali m'midzi yotetezedwa zedi ndi malinga ndi mayenje kapena kuseri kwa zipupa. Udani wawo pakati pawo ngwaukulu zedi. Ukhoza kuganiza kuti iwowo ngogwirizana chimodzi, koma kuti mitima yawo njosiyana. Izi n'chifukwa choti iwowo sazindikira lamulo la Allah ndipo saganizira ma Ayat Ake.]

(15) Fanizo (la Ayuda a Banu Nadhwiru) lili ngati amene adatsutsa mwa Ayuda (a Kainukaai) amene awatsogolera (kupeza mavuto) posachedwapa. Adalawa chilango cha zochita zawo chifukwa cha kusakhulupirira kwawo (ndi kuswa mapangano). Ndipo iwo adzalandira chilango (china) chowawa kwambiri (pa Tsiku Lachiweruzo).

[Fanizo la Ayuda amenewa pa zomwe zidawapeza za chilango cha Allah lili ngati fanizo la makafiri a Chiquraish tsiku la nkhondo ya Badr komanso Ayuda a Banu Qainuqaai omwe adalawa kuipa kwa mapeto a ukafiri wawo ndi udani wawo womuchitira Mtumiki (SAW) pa dziko la pansi ndikutinso ali nacho chilango chopweteka kwambiri Tsiku Lomaliza.]

(16) Fanizo la achiphanaso (pa kuwanyenga Banu Nadhwiri kuti amupandukire Mtumiki (SAW) wa Allah) lili ngati satana (ponyenga munthu kusiya chikhulupiriro) adati kwa iye: "Mkane (Allah)". Ndipo pamene adam'kana, (satana) adati, "Ine sindili ndi iwe; ndithu, ine ndikuopa Allah, Mbuye wa zolengedwa".

[Fanizo la achiphamaso amenewa powanyenga Ayuda zochita nkhondo ndi kuwalonjeza kwawo zowathandizira nkhondo polimbana ndi Mtumiki (SAW) wa Allah (SAW), lili ngati fanizo la satana pamene adamusalaliritsira munthu ukafiri nkumuitanira kumeneko. Pamene adachita ukafiri satana adanena kuti: "Ndithudi ine ndadzitalikitsa kwa iwe, ndithudi ine ndikuopa Allah Mbuye wa zolengedwaa zonse.]

(17) Choncho mapeto a onse awiriwo, kudali kukalowa ku moto ndi kukhala m'menemo muyaya. Iyi ndiyo mphoto ya anthu onyenga (ochenjerera anzawo).

[Ndiye mapeto a satana ndi munthu amene adamutsatira nkukanira (kuchita ukafiri) ndi akuti awiri onsewo akalowa ku moto n'kukakhalamo muyaya. Amenewo ndiwo malipiro a anthu opyola malire a Allah.]

(18) E, inu amene mwakhulupiririra! Muopeni Allah (potsatira malamulo Ake ndi kysiya zimene waletsa) ndipo munthu wina aliyense alingalire zimene watsogoza (kuti zikamuthandize) mawa. Muopeni Allah ndithudi Allah, ngodziwa zimene mukuchita (kotero adzakulipirani pa zimenezo).

[E, inu amene mudamuvomereza Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) motsimikiza ndi kugwiritsa ntchito malamulo Ake! Muopeni Allah, ndipo pewani chilango Chake pochita zimene wakulamulani ndi kusiya zimene wakuletsani. Ndipo mzimu uliwonse ulingalire ntchito zimene watsogoza zokonzekera Tsiku

Lakiyama. Ndipo muopeni Allah mu chirichonse chimene mukuchita kapena kusiya kuchichita. Ndithu Allah Subhaanahu ndi wozindikira zimene mukuchita, palibe kanthu kena kalikonse kangabisike mu ntchito zanu ndipo Iye ndi wodzakulipirani pa ntchitozo.]

(19) Ndipo musakhale monga amene aiwala zoyenera kumchitira Allah; (naye Allah) wawaiwalitsa mitima yawo (powalekerera kusazindikira zimene zingawathandize). Amenewa ndiwo olakwa kwakukulu (otuluka ku chilamulo cha Allah).

[Ndipo inu okhulupirira musakhale ngati anthu amene asiya kuchita zoyenera kumuchitira Allah zomwe adawalamula kuti atero; choncho pachifukwa chimenecho, adaiwalitsa mitima yawo kupeza gawo la zabwino zimene zingawapulumutse kuchilango cha Tsiku Lakiyama. Iwowa ndi anthu amene atenga mbiri zoipitsitsa, otuluka ndi kupandukira za kumvera Allah ndi Mtumiki Wake (SAW).

(20) Sangafanane anthu a ku moto (olangidwa) ndi anthu a ku Jannah (opeza mtendere); anthu a ku Jannah ndiwo opambana.

[Sangafanane anthu a ku moto olangidwa ndi anthu a ku Jannah opeza mtendere. Anthu a ku Jannah amenewo ndi opambana opeza kalikonse kofunikira komanso opulumuka ku chili chonse choipa.]

(21) Chikhala kuti tidaivumbulutsa Qur'aan iyi pamwamba pa phiri, ukadaliona phirilo lili lodzichepetsa ndi kung"ambika chifukwa choopa Allah. Awa ndi mafanizo amene tikuwapereka kwa anthu kuti aganizire.

[Tikadaivumbulutsa Qur'aaniyi pamwamba pa phiri limodzi mwa mapiri amene alipowa, phirilo ndikumvetsa zimene zili m'kati mwake za malonjezo abwino (kwa amene akuchita zabwino) ndi ziopsezo (za chilango kwa opandukira malamulo a Allah),bwenzi utaliona phirilo angakhale lili la mphamvu, lalikulu komanso lolimba, ukadaliona likudzichepetsa kwambiri ndikung'ambikang'ambika chifukwa choopa Allah Taalaa. Amenewa ndi mafanizo amene timawapereka ndikuwalongosolera anthu kuti alingalire za kuthekera kwa Allah ndi ukulu Wake. Mu ayat imeneyi mukupezekamo (lamulo) kuchitira khama zoilingalira Qur'aan ndi kumvetsa matanthauzo ake komanso kuigwiritsa ntchito.]

(22) Iye ndi Allah, Amene palibenso wina wopembedzedwa mwachoonadi koma Iye, Wodziwa za mseri ndi zooneka. Iye Ngwachifundo chambiri Ngwachisoni. [Iye ndi Allah Subhaanahu wopembedzedwa mwachoonadi amene palibe wina wopembedzedwa kupatula Iye, Wodziwa zobisika ndi zooneka. Akudziwa zimene zidabisika ndi zimene zilipo (kuonekera panthawiyo). Iye Ngwachifundo chambiri amene chifundo Chake chakwanira kanthu kalikonse. Iye Ngwachisoni ndi anthu amene ali ndi chikhulupiriro mwa Iye.]

(23) Iye ndi Allah, Amene palibenso wina wopembedzedwa mwachoonadi kupatula Iye,Mwini chili chonse, Woyera, Mwini mtendere, Wotsimikizira (atumiki Ake powapatsa mphamvu zochitira zozwizwitsa). Msungi wa chilichonse (Yemwe akuona zochita za anthu Ake) Wamphamvu zopambana, Mgonjetsi, Wotukuka mu ulemerero, Wamkulu. Wapatukana Allah ku zimene akumuphatikiza nazo.[Iye ndi wopembedzedwa mwachoonadi Amene palibe wina wopembedzedwa kupatula Iye, mwini wa zinthu zonse Amene amachita mwachifuniro Chake mu zolengedwa zonse popanda kukana kulikonse ngakhalenso kudzitchinjiriza kuli konse. Iye ndiwoyeretsedwa ku kupunguka kwa mtundu wina uliwonse; Amene wapatulika ku chiri chonse chonyansa. Iye ndi wotsimikizira atumiki ndi aneneri Ake kupyolera mzimene amatumiza nazo mu zozwizwitsa zoonekera. Iye ndi Muyang'aniri pa ntchito zonse za zolengedwa Zake zonse. Iye ndi Wamphamvu Yemwe sangagonjetsedwe, Mgonjetsi amene adagonjetsa akapolo (Ake) onse kotero zolengedwa zonse zagonjera kwa Iye ndikumumvera. Wodzikuza Amene ali nawo ulemerero ndi ukulu wina uli onse. Allah wapatulika ku zomwe amamuphatikiza Naye pomupembedza.]

(24) Iye ndi Allah; Mulengi wa (zinthu, palibe chomufanizira) Muumbi wa chilichonse, Mkozi wa maonekedwe a zinthu, Ake ndi maina abwino, zonse za kumwamba ndi pansi zikumulemekeza Iye ndi kumuyeretsa kumakhalidwe osayenerera ndi ulemerero Wake. Iye ndi Wopambana ndiponso Wanzeru zakuya

[Iye ndi Allah Subhaanahu Wa Taalaa Mulengi komanso Wokonzera zolengedwa Zake chilichonse, Muyambitsi, Wopanga ndi kuchititsa kuti zolengedwa zonse zipezeke malinga ndi nzeru Zake zakuya. Iye ndi Muumbi wa maonekedwe a zolengedwa Zake m'mene angafunire. Iye Subhaanahu ali nawo maina abwino komanso mbiri zapamwamba. Zimamuyeretsa Iye zonse zimene zili kumwamba komanso pa nthaka. Ndipo iye Ngwamphamvu amene amalanga adani Ake molapitsa, Ngwanzeru zakuya mukulinganiza Kwake kwa zinthu za zolengedwa Zake.]

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

يَٰٓأَيُّهَا ٱلَّذِينَ ءَامَنُواْ لَا تَتَّخِذُواْ عَدُوِّي وَعَدُوَّكُمۡ أَوۡلِيَآءَ تُلۡقُونَ
إِلَيۡهِم بِٱلۡمَوَدَّةِ وَقَدۡ كَفَرُواْ بِمَا جَآءَكُم مِّنَ ٱلۡحَقِّ يُخۡرِجُونَ ٱلرَّسُولَ
وَإِيَّاكُمۡ أَن تُؤۡمِنُواْ بِٱللَّهِ رَبِّكُمۡ إِن كُنتُمۡ خَرَجۡتُمۡ جِهَٰدٗا فِي سَبِيلِي
وَٱبۡتِغَآءَ مَرۡضَاتِيۚ تُسِرُّونَ إِلَيۡهِم بِٱلۡمَوَدَّةِ وَأَنَا۠ أَعۡلَمُ بِمَآ أَخۡفَيۡتُمۡ
وَمَآ أَعۡلَنتُمۡۚ وَمَن يَفۡعَلۡهُ مِنكُمۡ فَقَدۡ ضَلَّ سَوَآءَ ٱلسَّبِيلِ ١ إِن
يَثۡقَفُوكُمۡ يَكُونُواْ لَكُمۡ أَعۡدَآءٗ وَيَبۡسُطُوٓاْ إِلَيۡكُمۡ أَيۡدِيَهُمۡ وَأَلۡسِنَتَهُم
بِٱلسُّوٓءِ وَوَدُّواْ لَوۡ تَكۡفُرُونَ ٢ لَن تَنفَعَكُمۡ أَرۡحَامُكُمۡ وَلَآ أَوۡلَٰدُكُمۡۚ
يَوۡمَ ٱلۡقِيَٰمَةِ يَفۡصِلُ بَيۡنَكُمۡۚ وَٱللَّهُ بِمَا تَعۡمَلُونَ بَصِيرٞ ٣ قَدۡ
كَانَتۡ لَكُمۡ أُسۡوَةٌ حَسَنَةٞ فِيٓ إِبۡرَٰهِيمَ وَٱلَّذِينَ مَعَهُۥٓ إِذۡ قَالُواْ لِقَوۡمِهِمۡ
إِنَّا بُرَءَٰٓؤُاْ مِنكُمۡ وَمِمَّا تَعۡبُدُونَ مِن دُونِ ٱللَّهِ كَفَرۡنَا بِكُمۡ وَبَدَا بَيۡنَنَا
وَبَيۡنَكُمُ ٱلۡعَدَٰوَةُ وَٱلۡبَغۡضَآءُ أَبَدًا حَتَّىٰ تُؤۡمِنُواْ بِٱللَّهِ وَحۡدَهُۥٓ إِلَّا
قَوۡلَ إِبۡرَٰهِيمَ لِأَبِيهِ لَأَسۡتَغۡفِرَنَّ لَكَ وَمَآ أَمۡلِكُ لَكَ مِنَ ٱللَّهِ مِن شَيۡءٖۖ
رَّبَّنَا عَلَيۡكَ تَوَكَّلۡنَا وَإِلَيۡكَ أَنَبۡنَا وَإِلَيۡكَ ٱلۡمَصِيرُ ٤ رَبَّنَا لَا تَجۡعَلۡنَا
فِتۡنَةٗ لِّلَّذِينَ كَفَرُواْ وَٱغۡفِرۡ لَنَا رَبَّنَآۖ إِنَّكَ أَنتَ ٱلۡعَزِيزُ ٱلۡحَكِيمُ ٥

## (60) SUURATUL MUMTAHINAH

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) E, inu amene mwakhulupirira! Musawachite adani Anga ndi adani anu kukhala athandizi anu ndi kumawauza (nkhani zanu) mwa chikondi, pomwe iwo sanakhulupirire choonadi chimene chakudzerani. Adam'tulutsa Mtumiki (SAW) ndi inu nomwe (m'nyumba zanu) chifukwa chakuti mumakhulupirira Allah, Mbuye wanu (palibe cholakwa chilichonse chimene mudawachitira), ngati mwatuluka kukachita jihaad pa njira Yanga ndi kufunafuna chikondi Changa (musapalane nawo ubwenzi) mukuwatumizira chinsinsi (chanu cha nkhondo) chifukwa cha chikondi (chanu ndi iwo) pomwe Ine ndikudziwa zimene inu mukubisa ndi zimene mukuzisonyeza (poyera); amene akuchita zimenezi mwa inu ndiye kuti wataya njira yoongoka. [E, inu amene mudamuvomereza Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndikugwiritsa ntchito malamulo Ake! Musawachite adani Anga komanso adani anu kukhala osankhika ndi okondeka (anu), mukulumikizana nawo mwachikondi ndi kumawauza nkhani za Mtumiki (SAW) ndi za Asilamu ena onse. Iwowo adakanira zimene zidakudzerani mwachoonadi monga kukhulupirira mwa Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndi zomwe zavumbulutsidwa kwa iye za Qur'aan; akumam'tulutsa Mtumiki (SAW) ndi inu nomwe e, inu amene mudakhulupirira kuchoka mu Makka chifukwa choti inu mudamuvomereza Allah Mbuye wanu komanso mumavomereza umodzi Wake. Ngatidi inuyo – e, inu amene mudakhulupirira - mudasamuka komanso kuchita jihaad pa njira Yanga uku mukufuna chiyanjo Changa kwa inu, choncho musamayese abwenzi adani Anga komanso adani anu; mukulumikizana nawo mwachinsinsi pamene Ine ndikudziwa zimene mwazibisa komanso mwaonetsera. Amene angachite zimenezo mwa inu ndiye kuti wataya njira yachoonadi ndi yowona, komanso wasokera ku njira yolondola.]

(2) Akakumana nanu (pa nkhondo) akukhala adani anu, ndipo akukutambasulirani manja ndi malirime awo moipa (pokuthirani nkhondo ndi kukutukwanani) ndipo akulakalaka mukadakhala osakhulupirira (kuti mufanane nawo).

[Amene mukumalumikizana nawowo mwachikondi ndi mwamseri, akati akupezerereni, amakhala okuthirani nkhondo ndipo amatambasula manja awo kukuphani ndi kukugwira ukapolo, komanso malirirme awo pokutukwanani ndikukusambulani. Iwo amalakalaka nthawi zonse kuti mukadakhala makafiri monga iwo.]

(3) Abale anu ndi ana anu (amene mukukondana nawo pomwe ali adani a Allah ndi inu nomwe),sadzakuthandizani Tsiku Lakiyama (ndipo Allah) adzakusiyanitsani (tsiku limenelo), ndipo Allah akuona zimene mukuchita.[Maubale anu ngakhale ana anu sadzakuthandizani kanthu kalikonse pa nthawi imene inu mukupalana ubwenzi ndi makafiri pa chifukwa cha iwo. Allah adzalekanitsa pakati panu Tsiku Lakiyama ndipo adzalowetsa anthu omumvera ku Jannah ndipo anthu omunyoza ku moto. Palibe chobisika kwa Allah mu mawu anu komanso ntchito zanu.]

(4) Ndithu, inu muli ndi chitsanzo chabwino cha (Mtumiki) Ibrahim (AS) ndi amene adali naye pamene adauza anzawo (osakhulupirira kuti: ) "Ndithu, ife tapatukana nanu pamodzi ndi milungu yanu imene mukuipembedza kusiya Allah; takukanani, ndipo chidani ndi kusakondana zaonekera poyera pakati pa inu ndi ife mpaka muyaya, kufikira pamene mudzakhulupirira mwa Allah m'modzi", (inunso chitani chimodzimodzi, muwakane abale anu amene ali osakhulupirira mwa Allah) kupatula mawu a Ibrahim (AS) pamene adauza tate wake (kuti): "Ndithu, ndikupempherani chikhululuko. Palibe chimene

ndingakutetezereni nacho ku chilango cha Allah (ngati mutamuphatikiza Allah ndi zinthu zina”. (Mawu amenewo musatsatire koma pempherani motere:) “O, Mbuye wathu! Kwa Inu tatsamira ndipo kwa Inu tatembenukira ndiponso kobwerera nkwa Inu. [O, inu okhulupirira! Muli nacho chitsanzo chabwino choti nkutsatira mwa Ibrahim (AS) ndi anthu okhulupirira amene anali naye pamene adayankhula kwa anthu okanira Allah a mtundu wawo kuti: “Ife tapatukana ndi inu ndi zomwe mukupembedza zosakhala Allah, milungu yanu yopeka ndi mafano, ife takukanani, komanso tazikanitsitsa momwe mulili mukukanira kwanu Allah, ndipo udani ndikusakondana zaonekera pakati pathu ndi inu mpaka muyaya, mukamapitiirirabe pa ukafiri wanuwo kufikira mutakhulupirira mwa Allah Yekha. Koma kupemphererera chikhululukuko kwa Ibrahim (AS) pa tate wake zisalowe mu gawo la zitsanzo zabwino zotengera. Ndithudi zimenezi zinkachitika zisadadziwike bwino kwa Ibrahim (AS) kuti ndithu tate wakeyo ndi mdani wa Allah. Ndipo pamene zidadziwika kwa iye zoti ndi mdani wa Allah, adapatukana naye. Mbuye wathu! Tayadzamira pa Inu Nokha komanso tikubwerera kwa inu pakulapa kusiya machimo athu ndiponso kwa Inu ndikobwerera Tsiku Lakiyama.]

(5) O, Mbuye wathu! Musatichite kukhala mayeso a amene sadakhulupirire, tikhululukireni Mbuye wathu! Ndithu Inu, Ndinu Amphamvu zopambana ndiponso Anzeru zakuya.”

[Mbuye wathu! Musatichite ifeyo kukhala mayeserero a anthu okanira potipatsa chilango Chanu kapena kupatsa mphamvu makafiri pa ife angatipomphonetse ku chipembedzo chathu kapena kutigonjetsa ife, kuopera kuti angagwere m’mayesero ndi zimenezo, moti iwowa nkumadzanena kuti: “Adakakhala amenwa ali pa choonadi,sibwenzi chilango chimenechi chitawapeza.” Kotero iwo nkmaonjezereka ukafiri. Ndipo Inu Mbuye wathu! Tibisireni machimo athu ndi chikhululuko Chanu pa machimowo. Ndithu Inuyo ndi Wopambana amene sagonjetsedwa, Wanzeru zakuya mu zoyankhula Zake komanso zochita Zake.]

(6) Ndithu muli nacho mwa iwo chitsanzo chabwino (inu okhulupirira) kuchokera kwa Ibrahim (AS) ndi amene adali naye pakupatukana ndi adani a Allah; chitsanzo chimenechi) ndi cha aliyense amene akuyembekezera kukumana ndi Allah ndi Tsiku Lomaliza. Ndipo amene anyozere (kutsanzirako wadzichitira chiyengo yekha) ndithu Allah Ngokwanira m’kuyenera (ndipo) Ngoyamikidwa.

لَقَدْ كَانَ لَكُمْ فِيهِمْ أُسْوَةٌ حَسَنَةٌ لِّمَن كَانَ يَرْجُوا۟ ٱللَّهَ وَٱلْيَوْمَ ٱلْـَٔاخِرَ ۚ
وَمَن يَتَوَلَّ فَإِنَّ ٱللَّهَ هُوَ ٱلْغَنِىُّ ٱلْحَمِيدُ ﴿٦﴾ ۞ عَسَى ٱللَّهُ أَن يَجْعَلَ
بَيْنَكُمْ وَبَيْنَ ٱلَّذِينَ عَادَيْتُم مِّنْهُم مَّوَدَّةً ۚ وَٱللَّهُ قَدِيرٌ ۚ وَٱللَّهُ غَفُورٌ رَّحِيمٌ
﴿٧﴾ لَّا يَنْهَىٰكُمُ ٱللَّهُ عَنِ ٱلَّذِينَ لَمْ يُقَٰتِلُوكُمْ فِى ٱلدِّينِ وَلَمْ يُخْرِجُوكُم
مِّن دِيَٰرِكُمْ أَن تَبَرُّوهُمْ وَتُقْسِطُوٓا۟ إِلَيْهِمْ ۚ إِنَّ ٱللَّهَ يُحِبُّ ٱلْمُقْسِطِينَ
﴿٨﴾ إِنَّمَا يَنْهَىٰكُمُ ٱللَّهُ عَنِ ٱلَّذِينَ قَٰتَلُوكُمْ فِى ٱلدِّينِ وَأَخْرَجُوكُم
مِّن دِيَٰرِكُمْ وَظَٰهَرُوا۟ عَلَىٰٓ إِخْرَاجِكُمْ أَن تَوَلَّوْهُمْ ۚ وَمَن يَتَوَلَّهُمْ فَأُو۟لَٰٓئِكَ
هُمُ ٱلظَّٰلِمُونَ ﴿٩﴾ يَٰٓأَيُّهَا ٱلَّذِينَ ءَامَنُوٓا۟ إِذَا جَآءَكُمُ ٱلْمُؤْمِنَٰتُ
مُهَٰجِرَٰتٍ فَٱمْتَحِنُوهُنَّ ۖ ٱللَّهُ أَعْلَمُ بِإِيمَٰنِهِنَّ ۖ فَإِنْ عَلِمْتُمُوهُنَّ مُؤْمِنَٰتٍ
فَلَا تَرْجِعُوهُنَّ إِلَى ٱلْكُفَّارِ ۖ لَا هُنَّ حِلٌّ لَّهُمْ وَلَا هُمْ يَحِلُّونَ لَهُنَّ ۖ وَءَاتُوهُم
مَّآ أَنفَقُوا۟ ۚ وَلَا جُنَاحَ عَلَيْكُمْ أَن تَنكِحُوهُنَّ إِذَآ ءَاتَيْتُمُوهُنَّ أُجُورَهُنَّ ۚ
وَلَا تُمْسِكُوا۟ بِعِصَمِ ٱلْكَوَافِرِ وَسْـَٔلُوا۟ مَآ أَنفَقْتُمْ وَلْيَسْـَٔلُوا۟ مَآ أَنفَقُوا۟ ۚ
ذَٰلِكُمْ حُكْمُ ٱللَّهِ ۖ يَحْكُمُ بَيْنَكُمْ ۚ وَٱللَّهُ عَلِيمٌ حَكِيمٌ ﴿١٠﴾ وَإِن فَاتَكُمْ
شَىْءٌ مِّنْ أَزْوَٰجِكُمْ إِلَى ٱلْكُفَّارِ فَعَاقَبْتُمْ فَـَٔاتُوا۟ ٱلَّذِينَ ذَهَبَتْ
أَزْوَٰجُهُم مِّثْلَ مَآ أَنفَقُوا۟ ۚ وَٱتَّقُوا۟ ٱللَّهَ ٱلَّذِىٓ أَنتُم بِهِۦ مُؤْمِنُونَ ﴿١١﴾

[E, inu okhulupirira! Muli nacho chitsanzo choyamikika mwa Ibrahim (AS) ndi anthu amene anali naye, izi zili mwa amene akufuna zabwino za dziko lapansili komanso Tsiku Lomaliza. Tsono amene anyozere zimene Allah wamulangiza nazo zotengera zitsanzo zabwino za aneneri Ake, nkumapalana ubwenzi ndi adani Ake,ndiyetu Allah Ngolemera sasowekera kanthu kwa akapolo Ake, Woyamikidwa mu uchenicheni Wake komanso mbiri Zake, Wotamandika nthawi zonse.]

(7) Mwina Allah angaike chikondi pakati panu ndi ena mwa amene mumawada (poongolera mitima yawo kukhulupirira mwa Allah) Allah Ngokhoza chilichonse ndiponso Allah Ngokhululuka,Ngwachisoni.

[Nkutheka Allah kuika pakati pa inu amene mudakhulupirira ndi anthu amene mudachita nawo udani mwa achibale anu a mu anthu opembedza mafano chikondi pambuyo pa chidani komanso kuchitirana chisoni pambuyo pankhwidzi potsanula mitima yawo ku Chisilamu. Ndipo Allah ali nako kuthekera pa chinthu china chilichonse, ndipo Allah Ngokhululukira akapolo Ake,Ngwachisoni ndi iwo].

8 Allah sakukuletsani kuwachitira zabwino ndi chilungamo amene sadakuthireni nkhondo ndi kukutulutsani m'nyumba zanu chifukwa cha chipembedzo. Ndithu Allah amakonda (anthu) achilungamo. [E, inu okhulupirira! Allah sakukuletsani za omwe sadakuthireni nkhondo mwa makafiri chifukwa cha chipembedzo, ndipo sadakutulutseni m'nyumba zanu, kuwalemekeza kuwachitira zabwino, ndi kuchita chilungamo, powachitira zabwino za mtundu wina uli wonse. Ndithu Allah amakonda anthu amene amachita chilungamo pa zoyankhula komanso zochita zawo.]

9 Allah akukuletsani kugwirizana nawo amene adakuthirani nkhondo chifukwa cha chipembedzo ndi kukutulutsani m'nyumba zanu, ndi amene adathandiza kukutulutsani. Amene ati agwirizane nawo, iwowo ndiwo achinyengo.

[Ndithudi Allah akukuletsani za anthu amene adakuthirani nkhondo chifukwa cha chipembedzo, ndikuti adakutulutsani m'nyumba zanu ndipo adathandiza makafiri kukutulutsani, kuti muchite nawo ubwenzi mothandizana nawo pa nkhondo komanso mwachikondi. Amene awachite amenewa othandizana komanso okondeka awo polimbana ndi anthu okhulupirira, ndiye kuti iwowo ndi odzipondereza okha, otuluka m'malamulo a Allah.]

10 E, inu amene mwakhulupirira! Akakudzerani Asilamu achikazi osamuka, ayeseni mayeso (kuti mudziwe chikhulupiriro chawo); Allah ali wodziwa kwambiri za chikhulupiriro chawo. Ngati mutawadziwa kuti ndi okhulupirira, musawabwezere kwa osakhulupirira. Akaziwo saloledwa kukwatiwa ndi osakhulupirira, iwonso saloledwa kuwakwatira. Abwezereni chiongo chimene adapereka amuna osakhulupirirawo. Ndiye palibe tchimo kwa inu kuwakwatira, (ngakhale adasiya amuna awo achikafiri ku Makka) ngati muwapatsa chiongo chawo. Ndipo musakangamire maukwati ndi akazi achikafiri (osakhulupirira amene adatsalira ku Makka). Itanitsani zimene mudapereka kwa akazi anu (achikafiriwo), naonso akafiri aitanitse zimene adapereka (kwa akazi awo akalowa Chisilamu). Limenelo ndi lamulo la Allah limene akulamula pakati panu. Ndipo Allah ndi Wodziwa kwambiri ndiponso Ngwanzeru zakuya.

[E, inu amene mudamuvomera Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndikugwiritsa ntchito malamulo Ake! Akakudzerani akazi okhulupirira akusamuka kuchokera ku nyumba za chikafiri kupita ku nyumba za Chisilamu, ayeseni mayeso kuti mudziwe kuona kwa chikhulupiriro chawocho. Allah akudziwa kwambiri zoona zache za chikhulupiriro chawo. Ngati mutawadziwa kuti iwowo ndi okhulupirira malinga ndi zomwe zingaonekere kwa inu mu zisonyezo ndi maumboni, ndiye nusawabwezere kwa amuna awo achikafiri. Popeza akazi okhulupirira saloledwa kuwakwatira makafiri, chimodzimodzinso sizikuvomerezedwa kuwakwatira akazi okhulupirira. Apatseni akazi amene alowa Chisilamu zofanana ndi zomwe amuna awo achikafiri adaperekera chiongo kwa iwo. Palibe tchimo kwa inu kuti muwakwatire ngati mutawapatsa chiongo chawo. Ndipo musakakamire ukwati wa akazi anu achikafiri, komanso auzeni opembedza mafano zomwe mudapereka zokhudzana chiongo cha akazi anu amene adatuluka Chisilamu nkupita kwa makafiri. Nawonso aitanitse chiongo chimene adapereka kwa akazi awo amene alowa Chisilamu nadza kwa inu. Lamulo limene latchulidwali mu Ayat imeneyi ndi lamulo la Allah akulamulira nalo pakati panu, choncho musatsutsane nalo. Ndipo Allah amadziwa kwambiri, palibe chobisika kwa Iye, Wanzeru zakuya pa mawu Ake komanso ntchito Zake.]

11 Ngati m'modzi mwa akazi anu atakuthawani kupita kwa akafiri, ndipo (mwadzidzidzi) mwakachita nkhondo (ndi kupeza chuma chosiya adani anu), apatseni amene awathawa akazi awo chofanana ndi chimene adapereka (pokwatira). Ndipo muopeni Allah amene inu mukum'khulupirira.

[Ngati ena mwa akazi anu amene atuluka Chisilamu atapita kwa makafiri, ndipo makafiri sadakupatseni chiongo chomwe mudawapatsa akaziwo, kenako inu nkuwagonjetsa makafiri amenewo kapena ena osakhala iwo ndikuwapambana, apatseni anthu amene akazi awo adapita kuchoka m'gulu la Asilamu chuma chochipeza pa nkhondo kapena china chake chofanana ndi chiongocho izi zisadachitike. Ndipo muopeni Allah amene inuyo mudamukhulupirira.]

12 E, iwe Mtumiki (SAW)! Akakudzera akazi osakhulupirira kudzakulonjeza kuti sam'phatikiza Allah ndi chilichonse ndi kuti saziba, sazichita chiwerewere, sazipha ana awo, ndikuti sazinena bodza lamkunkhuniza lomwe akulipeka pakati pa manja awo ndi miyendo yawo (pom'pachika mwana kwa wina amene sali tate wake) ndikutinso sadzakunyoza pa chinthu chabwino (chimene ukuwaitanira), landira lonjezo lawolo ndipo

apemphere chikhululuko kwa Allah, ndithu Allah Ngokhululuka kwambiri, Ngwachisoni.

[E, iwe Mtumiki (SAW)! Ngati atadza kwa iwe akazi okhulupirira Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) akudzakulonjeza kuti sazichita pamodzi ndi Allah chomphatikiza nacho popembedza Iye, ndikuti saziba, ndipo sazichita chiwerewere, komanso sazipha ana awo akabadwa kumene kapena asanabadwe (kuchotsa pakati), ndikutinso saziwapachika amuna awo ana amene sali awo, kudzanso kuti sadzisemphana nawe maganizo pa zinthu zabwino zimene ungalamule nazo, ndiye kuti landira malonjezo awowo ndipo uwapempherere chikhululuko kwa Allah. Ndithu Allah Ngokhululuka machimo a akapolo Ake olapa komanso Ngwachisoni ndi iwo.]

13 E, inu amene mwakhulupirira! musagwirizane ndi anthu amene Allah adawakwiyira ndipo ataya mtima wopeza mphoto Tsiku Lomaliza (chifukwa cha machimo awo ochuluka) monga momwe atayira mtima akafiri za kuuka kwa amene ali m'manda

[E, inu amene mudakhulupirira mwa Allah ndi Mtumiki Wake (SAW)! Musawachite anthu amene Allah adawakwiyira chifukwa cha ukafiri wawo kukhala abwenzi, komanso okondana nawo. Iwowo adataya mtima za malipiro a Allah a Tsiku Lomaliza monga m'mene adataira mtima makafiri amene ali m'manda za chisoni cha Allah, pamene adaona zoona zake, ndikudziwa kotsimikiza kuti ndithu iwowo alibe gawo lili lonse lakumeneko; kapena momwe adataira mtima makafiri zoukanso m'manda – anthu akufa - chifukwa cha chitsimikizo chawo choti kulibenso kuuka kwa akufa.]

## (61) SUURATU –AS-SWAFF

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Zonse zakumwamba ndi za pansi zimalemekeza Allah (ndi kumuyeretsa kumakhalidwe osayenera ndi ulemerero Wake). Ndipo Iye Ngopambana pa chilichonse, Ngwanzeru zakuya.

[Zomwe zili kumwamba komanso zili pansi zimamuyeretsa Allah ku zonse zimene zili zosayenerera ndi Iyeyo. Ndipo Iye Ngopambana amene sagonjetsedwa, Wanzeru zakuya mu zoyankhula Zake komanso zochita Zake.]

2 E, inu amene mudakhulupirira! Bwanji mukunena zimene simumachita?

[E, inu amene mudamuvomereza Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndi kugwiritsa ntchito malamulo Ake! N'chifukwa chiyani mukumalonjeza lonjezo kapena kunena liwu

يَٰٓأَيُّهَا ٱلنَّبِيُّ إِذَا جَآءَكَ ٱلۡمُؤۡمِنَٰتُ يُبَايِعۡنَكَ عَلَىٰٓ أَن لَّا يُشۡرِكۡنَ
بِٱللَّهِ شَيۡـٔٗا وَلَا يَسۡرِقۡنَ وَلَا يَزۡنِينَ وَلَا يَقۡتُلۡنَ أَوۡلَٰدَهُنَّ وَلَا يَأۡتِينَ
بِبُهۡتَٰنٖ يَفۡتَرِينَهُۥ بَيۡنَ أَيۡدِيهِنَّ وَأَرۡجُلِهِنَّ وَلَا يَعۡصِينَكَ
فِي مَعۡرُوفٖ فَبَايِعۡهُنَّ وَٱسۡتَغۡفِرۡ لَهُنَّ ٱللَّهَۚ إِنَّ ٱللَّهَ غَفُورٞ رَّحِيمٞ
١٢ يَٰٓأَيُّهَا ٱلَّذِينَ ءَامَنُواْ لَا تَتَوَلَّوۡاْ قَوۡمًا غَضِبَ ٱللَّهُ عَلَيۡهِمۡ
قَدۡ يَئِسُواْ مِنَ ٱلۡأٓخِرَةِ كَمَا يَئِسَ ٱلۡكُفَّارُ مِنۡ أَصۡحَٰبِ ٱلۡقُبُورِ ١٣

ترتيبها ٦١ — سُورَةُ الصَّفِّ — آياتها ١٤

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

سَبَّحَ لِلَّهِ مَا فِي ٱلسَّمَٰوَٰتِ وَمَا فِي ٱلۡأَرۡضِۖ وَهُوَ ٱلۡعَزِيزُ ٱلۡحَكِيمُ
١ يَٰٓأَيُّهَا ٱلَّذِينَ ءَامَنُواْ لِمَ تَقُولُونَ مَا لَا تَفۡعَلُونَ ٢
كَبُرَ مَقۡتًا عِندَ ٱللَّهِ أَن تَقُولُواْ مَا لَا تَفۡعَلُونَ ٣ إِنَّ
ٱللَّهَ يُحِبُّ ٱلَّذِينَ يُقَٰتِلُونَ فِي سَبِيلِهِۦ صَفّٗا كَأَنَّهُم
بُنۡيَٰنٞ مَّرۡصُوصٞ ٤ وَإِذۡ قَالَ مُوسَىٰ لِقَوۡمِهِۦ يَٰقَوۡمِ لِمَ
تُؤۡذُونَنِي وَقَد تَّعۡلَمُونَ أَنِّي رَسُولُ ٱللَّهِ إِلَيۡكُمۡۖ فَلَمَّا
زَاغُوٓاْ أَزَاغَ ٱللَّهُ قُلُوبَهُمۡۚ وَٱللَّهُ لَا يَهۡدِي ٱلۡقَوۡمَ ٱلۡفَٰسِقِينَ ٥

lomwe simumalikwaniritsa kulichita? Uku ndikunyazitsa anthu amene zoyankhula zawo zimasemphana ndi zochita zawo.]

3 Allah amakuda zedi kunena zinthu zomwe simumachita.

[Kwakula kudedwa kwa Allah kuti muziyankhula ndi malirime anu zomwe simumazichita.]

4 Ndithu, Allah akukonda amene akumenya nkhondo pa njira Yake yofalitsa chipembedzo (Chake) ali pa mzere (umodzi) uku ali monga chomanga chomangika mwamphamvu.

[Ndithu Allah amakonda anthu amene akumenya nkhondo pa njira Yake, ali pa mzere umodzi ngati nyumba yogwirana yomangika bwino mwamphamvu moti sangazembemo adani. Mu ayat imeneyi muli kufotokoza ubwino wa jihaad ndi anthu ochita jihaad chifukwa cha chikondi cha Allah Subhaanahu kwa akapolo Ake okhulupirira akaima pa mzere molunjika adani a Allah nkumamenyana nawo pa njira Yake.]

5 (Ndipo kumbuka iwe Muhammad (SAW) ) pamene Mussa (AS) adawauza anthu ake kuti: "E, inu anthu anga! Bwanji mukundizunza,

وَإِذْ قَالَ عِيسَى ٱبْنُ مَرْيَمَ يَٰبَنِىٓ إِسْرَٰٓءِيلَ إِنِّى رَسُولُ ٱللَّهِ إِلَيْكُم مُّصَدِّقًا
لِّمَا بَيْنَ يَدَىَّ مِنَ ٱلتَّوْرَىٰةِ وَمُبَشِّرًۢا بِرَسُولٍ يَأْتِى مِنۢ بَعْدِى ٱسْمُهُۥٓ أَحْمَدُ ۖ فَلَمَّا
جَآءَهُم بِٱلْبَيِّنَٰتِ قَالُوا۟ هَٰذَا سِحْرٌ مُّبِينٌ ﴿٦﴾ وَمَنْ أَظْلَمُ مِمَّنِ ٱفْتَرَىٰ
عَلَى ٱللَّهِ ٱلْكَذِبَ وَهُوَ يُدْعَىٰٓ إِلَى ٱلْإِسْلَٰمِ ۚ وَٱللَّهُ لَا يَهْدِى ٱلْقَوْمَ ٱلظَّٰلِمِينَ
﴿٧﴾ يُرِيدُونَ لِيُطْفِـُٔوا۟ نُورَ ٱللَّهِ بِأَفْوَٰهِهِمْ وَٱللَّهُ مُتِمُّ نُورِهِۦ وَلَوْ كَرِهَ
ٱلْكَٰفِرُونَ ﴿٨﴾ هُوَ ٱلَّذِىٓ أَرْسَلَ رَسُولَهُۥ بِٱلْهُدَىٰ وَدِينِ ٱلْحَقِّ لِيُظْهِرَهُۥ
عَلَى ٱلدِّينِ كُلِّهِۦ وَلَوْ كَرِهَ ٱلْمُشْرِكُونَ ﴿٩﴾ يَٰٓأَيُّهَا ٱلَّذِينَ ءَامَنُوا۟ هَلْ أَدُلُّكُمْ
عَلَىٰ تِجَٰرَةٍ تُنجِيكُم مِّنْ عَذَابٍ أَلِيمٍ ﴿١٠﴾ تُؤْمِنُونَ بِٱللَّهِ وَرَسُولِهِۦ وَتُجَٰهِدُونَ
فِى سَبِيلِ ٱللَّهِ بِأَمْوَٰلِكُمْ وَأَنفُسِكُمْ ۚ ذَٰلِكُمْ خَيْرٌ لَّكُمْ إِن كُنتُمْ تَعْلَمُونَ ﴿١١﴾
يَغْفِرْ لَكُمْ ذُنُوبَكُمْ وَيُدْخِلْكُمْ جَنَّٰتٍ تَجْرِى مِن تَحْتِهَا ٱلْأَنْهَٰرُ وَمَسَٰكِنَ
طَيِّبَةً فِى جَنَّٰتِ عَدْنٍ ۚ ذَٰلِكَ ٱلْفَوْزُ ٱلْعَظِيمُ ﴿١٢﴾ وَأُخْرَىٰ تُحِبُّونَهَا ۖ نَصْرٌ
مِّنَ ٱللَّهِ وَفَتْحٌ قَرِيبٌ ۗ وَبَشِّرِ ٱلْمُؤْمِنِينَ ﴿١٣﴾ يَٰٓأَيُّهَا ٱلَّذِينَ ءَامَنُوا۟ كُونُوٓا۟
أَنصَارَ ٱللَّهِ كَمَا قَالَ عِيسَى ٱبْنُ مَرْيَمَ لِلْحَوَارِيِّۦنَ مَنْ أَنصَارِىٓ إِلَى ٱللَّهِ ۖ
قَالَ ٱلْحَوَارِيُّونَ نَحْنُ أَنصَارُ ٱللَّهِ ۖ فَـَٔامَنَت طَّآئِفَةٌ مِّنۢ بَنِىٓ إِسْرَٰٓءِيلَ
وَكَفَرَت طَّآئِفَةٌ ۖ فَأَيَّدْنَا ٱلَّذِينَ ءَامَنُوا۟ عَلَىٰ عَدُوِّهِمْ فَأَصْبَحُوا۟ ظَٰهِرِينَ ﴿١٤﴾

chikhalirecho mukudziwa kuti ine ndine Mtumiki wa Allah kwa inu?" Ndipo pamene adapitiriza kupandukira choonadi, Allah adaipinda mitima yawo (kuti isalandire chiongoko). Ndipo Allah saongola anthu otuluka m'chilamulo Chake.

[Iwe Mtumiki (SAW)! Afotokozere anthu ako za nthawi imene adayankhula Mussa (AS) kwa anthu ake kuti: "Ndi chifukwa chiyani mukundizunza ndi mawu komanso ndi zochita, kumachita kuti mukudziwa kuti ndinedi ndi Mtumiki wa Allah?" Pamene adapotoka kusiya choonadi uku akudziwa za icho, nakakamira pa izo, Allah adachotsa mitima yawo kuti isalandire choonadi kukhala chilango cha kupotoka kwawo kumene adadzisankhila okha. Ndipo Allah saongola anthu otuluka mu kumvera Iye komanso njira yoona.]

6 Ndiponso (kumbuka) pamene adanena (Mtumiki) Issa mwana wa Mariam (AS) kuti: "E, inu ana a Israeli! Ine ndine Mtumiki wa Allah kwa inu, wochitira umboni zimene zidadza patsogolo panga za Buku Lachipangano Chakale (Torah) ndipo ndkukuuzani nkhani yabwino ya Mtumiki amene adzadza pambuyo panga dzina lake Ahmad (Muhammad SAW)." [Iwe Mtumiki (SAW)! Afotokozere anthu ako nthawi imene Issa mwana wa Mariam (AS) adanena kwa anthu ake kuti: "Ndithudi ine ndi Mtumiki wa Allah kwa inu, ndikuchitira umboni zimene zidadza patsogolo panga, za Buku Lachipangano Chakale – (Torah) komanso kudzaikiranso umboni za kuwona kwa mtumiki amene akudza pambuyo panga dzina lake Ahmad yemwe ndi Muhammad (SAW) ndi kudzakuitanirani inuyo kuti mudzamvomereze. Pamene Muhammad (SAW) adadza kwa iwo ndi ma-Ayat Olongosola momveka adanena kuti: "Izi zimene watibweretsera ndi ufiti wowonekeratu poyera."]

7 Kodi ndi ndani woipitsitsa kupondereza kuposa wopekera Allah bodza, pomwe iye akuitanidwa ku Chisilamu (chipembedzo choona ndi chabwino) ndipo Allah saongola anthu achinyengo. [Ndipo palibe wina aliyense wopyoza muyeso popondereza ndi kupandukira woposa amene wapekera Allah bodza namuchitira Iye ena om'phatikiza limodzi Naye pomupembedza. Ndipo iye akuitanidwa ku zoti alowe Chisilamu ndikuyeretsa mapemphero onse kwa Allah Yekhayo. Ndipo Allah samathandiza anthu amene adadzipondereza okha pochita ukafiri ndi kum'chitira Iye mafano ku zinthu zomwe muli kupambana kwawo.]

8 (Ana a Israeli akunenera zabodza Allah) ndicholinga chakuti azimitse kuunika kwa chipembedzo Chake ndi pakamwa pawo; (ndipo akufanana ndi amene akufuna kuzima kuunika kwa dzuwa pouzira ndi mpweya wa pakamwa pake); ndithu Allah akwaniritsa kuunika Kwake ngakhale osakhulupirira zikuwaipira. [Chimene akufuna anthu amenewa ndichoti afafanize choonadi chimene adatumizidwa nacho Muhammad (SAW) chomwe ndi Qur'aan ndi mawu awo abodza. Ndipo Allah achionetsera poyera choonadi pokwaniritsa chipembedzo Chake ngakhale atadana nazo anthu okanirawa, abodza.]

9 Iye ndi Amene adatuma Mtumiki Wake (Muhammad SAW) ndi chipembedzo choona kuti achiike pamwamba pa zipembedzo zonse, ngakhale kuti ophatikiza mafano ndi Allah zikuwaipira. [Iye ndi Amene adatumiza Mtumiki Wake Muhammad (SAW) ndi Qura'n ndi chipembedzo cha Chisilamu kuti achiike pamwamba pa zipembedzo zotsusana nacho, ngakhale anthu opembedza mafano adane nazo zimenezo.]

10 E, nu amene mudakhulupirira! Kodi ndikudziwitseni malonda amene angakupulumutseni ku chilango chowawa?

[E, inu anthu amene mudamuvomereza Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndi kugwiritsa ntchito malamulo Ake! Kodi ndikuongolereni ku malonda akulu kwambiri amene angakakupulumutseni ku chilango chopweteka?]

11 Muzim'khuluprira Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndiponso muzichita jihaad pa njira ya Allah ndi chuma chanu komanso matupi anu. Zimenezo n'zabwino kwa inu ngati muli odziwa.

[Muzipitiriza pa chikhulupiriro chanu mwa Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) komanso muzichita jihaad pa njira ya Allah poteteza chipembedzo Chake kudzera mu zimene muli nazo,chuma ndi miyoyo, zimenezi ndi zabwino kwa inu kuposa malonda a dziko lapansi, ngatidi mukudziwa kuipa kwa zinthu ndi ubwino wake, ndiye tsatirani zimenezo.]

12 Akukhululukirani machimo anu ndipo adzakakulowetsani m'minda momwe mitsinje ikuyenda pansi pake, ndiponso (adzakupatsani) mokhala mwabwino ku minda yamuyaya; kumeneko ndiko kupambana kwakukulu.

[E, inu okhulupirira! Ngati mutachita zimene wakulamulani Allah, akubisirani machimo anu ndikukakulowetsani ku minda yomwe ikuyenda pansi pa mitengo yake mitsinje ndi malo okhala abwino, oyenera ku minda yamtendere kokhalako muayaya mosadukiza. Kumeneko ndiko kupambana kumene palibenso kupambana kwina pambuye pake.]

13 Ndiponso zina zomwe mukuzikonda, thandizo lochokera kwa Allah ndi kugonjetsa kumene kuli pafupi; ndipo auze Asilamu nkhani yabwino.

[Ndipo chisomo ndi mtendere wina kwa inu okhulupirira umene mungaukonde, ndi kupambana kochokera kwa Allah kumene kukupezeni komanso chigonjetso chamsanga chimene chikwaniritsidwe m'manja mwanu. Ndipo iwe Mtumiki (SAW) auze okhukupirira nkhani yabwino yopambana ndikugonjetsa pa dziko la pansi komanso jannat pa Tsiku Lomaliza.]

14 E, inu amene mwakhulupirira!Khalani othangata kufalitsa chipembedzo cha Allah (pamene Mtumiki (SAW) akukuitananі kuti mum''mthangate) monga momwe adanenera Issa mwana wa Mariam (AS) powauza otsatira ake kuti: "Ndani adzandithangata pa ntchito ya Allah (yofalitsa chipembedzo Chake?") Otsatira ake adanena kuti : "Ife ndife othangata (kufalitsa chipembedzo cha) Allah." Choncho gulu lina la ana a Israeli lidakhulupirira, ndipo gulu lina silidakhulupirire, tero tidawapatsa mphamvu amene adakhulupirira pa adani awo, ndipo adali opambana.

[E, inu anthu amene mudamuvomereza Allah ndi Mtumiki (SAW) ndikugwiritsa ntchito malamulo Ake! Khalani athandizi a chipembedzo cha Allah ngati m'mene adalili odzipereka a Issa (AS) othandiza chipembedzo cha Allah pamene Issa (AS) adanena kwa iwo kuti: "Ndani mwa inu agwire ntchito yothandiza ine ndikundithangata ku zinthu zimene zingayandikitse kwa Allah? Iwo adati: "Ife ndi athandizi a chipembedzo cha Allah, kotero kadaongoka kagulu kena ka ana a Israeli pamene kena kadasokera. Ndiye Ife tidathandiza anthu amene adakhulupirira mwa Allah ndi Mtumiki Wake (SAW), ndipo tinathangata kugonjetsa amene adawachita adani m'magulu a Akhristu, kotero adakhala opambana pa iwo, zonsezi zidachitika pomutumiza Muhammad (SAW).]

## (62) SUURATUL JUM'A

سُورَةُ الجُمُعَةِ — ترتيبها ٦٢ — آياتها ١١

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَٰنِ الرَّحِيمِ

يُسَبِّحُ لِلَّهِ مَا فِي السَّمَاوَاتِ وَمَا فِي الْأَرْضِ الْمَلِكِ الْقُدُّوسِ الْعَزِيزِ
الْحَكِيمِ ١ هُوَ الَّذِي بَعَثَ فِي الْأُمِّيِّينَ رَسُولًا مِّنْهُمْ يَتْلُوا
عَلَيْهِمْ آيَاتِهِ وَيُزَكِّيهِمْ وَيُعَلِّمُهُمُ الْكِتَابَ وَالْحِكْمَةَ وَإِن كَانُوا
مِن قَبْلُ لَفِي ضَلَالٍ مُّبِينٍ ٢ وَآخَرِينَ مِنْهُمْ لَمَّا يَلْحَقُوا بِهِمْ
وَهُوَ الْعَزِيزُ الْحَكِيمُ ٣ ذَٰلِكَ فَضْلُ اللَّهِ يُؤْتِيهِ مَن يَشَاءُ وَاللَّهُ
ذُو الْفَضْلِ الْعَظِيمِ ٤ مَثَلُ الَّذِينَ حُمِّلُوا التَّوْرَاةَ ثُمَّ لَمْ
يَحْمِلُوهَا كَمَثَلِ الْحِمَارِ يَحْمِلُ أَسْفَارًا بِئْسَ مَثَلُ الْقَوْمِ
الَّذِينَ كَذَّبُوا بِآيَاتِ اللَّهِ وَاللَّهُ لَا يَهْدِي الْقَوْمَ الظَّالِمِينَ ٥
قُلْ يَا أَيُّهَا الَّذِينَ هَادُوا إِن زَعَمْتُمْ أَنَّكُمْ أَوْلِيَاءُ لِلَّهِ مِن
دُونِ النَّاسِ فَتَمَنَّوُا الْمَوْتَ إِن كُنتُمْ صَادِقِينَ ٦ وَلَا يَتَمَنَّوْنَهُ
أَبَدًا بِمَا قَدَّمَتْ أَيْدِيهِمْ وَاللَّهُ عَلِيمٌ بِالظَّالِمِينَ ٧ قُلْ إِنَّ
الْمَوْتَ الَّذِي تَفِرُّونَ مِنْهُ فَإِنَّهُ مُلَاقِيكُمْ ثُمَّ تُرَدُّونَ
إِلَىٰ عَالِمِ الْغَيْبِ وَالشَّهَادَةِ فَيُنَبِّئُكُم بِمَا كُنتُمْ تَعْمَلُونَ ٨

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Zonse za kumwamba ndi dziko lapansi zikulemekeza Allah, Mfumu Yoyera, Wamphamvu zopambana ndiponso Wanzeru zakuya (ndi kumuyeretsa ku makhalidwe

osayenerera ndi ulemerero Wake).
[Zikuyeretsa Allah Taalaa zili zonse zimene zili kumwamba komanso pa dziko lapansi ku zinthu zosayenerera ndi ulemerero Wake, Iye Yekhayo ndiye mwini wa china chilichonse, Amene amachita nazo m'mene angafunire popanda wotsutsana Naye, Wotalikitsidwa ku kukupunga kwa mtundu wina uli wonse. Wamphamvu zopambana Amene sagonjetsedwa, Wanzeru zakuya pakulinganiza Kwake ndi zochita Zake.]

2 Iye ndi amene adatumiza kwa Arabu (osadziwa kulemba ndi kuwerenga), Mtumiki (SAW) wochokera mwa iwo kuti awawerengere ndime Zake ndikuti awayeretse (ku uchimo ndi kumakhalidwe oipa) ndi kuwaphunzitsa Qur'aan ndi mawu anzeru (a Mtumiki SAW) ngakhale kuti kale adali osokera kowonekera (Mtumiki SAW) asadadze kwa iwo).
[Allah Subhaanahu wa Taalaa ndi Amene adatumiza kwa a Arab amene sadali kulemba ndi kuwerenga ndipo kwa iwo adalibe buku ngakhalenso chisonyezo chilichonse cha utumiki, Mtumiki (SAW) wochokera mwa iwo kwa anthu onse. Akumawerengera Qur'aan ndi kumawayeretsera zikhulupiriro zoonongeka ndi makhalidwe oipa. Ndikuwaphunzitsa Qur'aan komanso Sunnat za Mtumiki (SAW). Ndithu iwowo asadatumizidwe Mtumikiyu (SAW) adali mu kupotoka ku choonadi kowonekeratu.]

3 Ndipo (adam'tumizanso) kwa ena mwa iwo, omwe sadakumane nawo. Ndipo Iye (Allah) Ngopambana (pa chinthu chilichonse), Ngwamphamvu zoposa (ndiponso) Ngwanzeru zakuya.
[Ndipo Allah Subhaanahu adamutumiza kwa anthu ena amene sadadze, ndipo adzabwera ochokera mwa ma Arab ndi ena osakhala iwo. Ndipo Allah Yekhayo Ngwamphamvu, Wogonjetsa chinthu chili chonse, Ngwanzeru zakuya mu zoyankhula Zake ndi zochita Zake zomwe.]

4 Umenewo ndiwo ubwino wa Allah, akuupereka kwa amene wam'funa (mwa akapolo Ake) ndipo Allah yekha ndi Mwini ubwino waukulu. [Kutumiza Mtumikiyo (SAW) mu fuko la a Arab ndi ena osakhala iwo, ndi ubwino wa Allah, amam'patsa amene wam'funa mwa akapolo Ake. Iye Yekhayo ndi Wopambana pa zinthu zina zili zonse, Wanzeru zakuya mu zoyankhula Zake ndi zochita Zake.]

5 Fanizo la (Ayuda) amene adawasenzetsa Taurat (Chipangano Chakale, pokakamizidwa kuti atsatire zophunzitsa za bukulo, koma osatsatira), ali ngati bulu amene akusenza mabuku akuluakulu anzeru, (koma osathandizidwa nawo). Taonani kuipa fanizo la anthu otsutsa zisonyezo za Allah. Ndipo Allah saongola anthu achinyengo.
[Fanizo la Ayuda amene adakakamizidwa kugwiritsa ntchito Taurat kenako iwo napanda kuigwiritsira ntchito, lili ngati fanizo la bulu amene wanyamula mabuku asakudziwa zimene zili m'menemo. N''lonyansa zedi fanizo la anthu amene adakanira zizindikiro za Allah napanda kuthandizidwa nazo. Ndipo Allah sadalitsa anthu opondereza, amene amapyola malire Ake ndi kumatuluka mu kumumvera Iye.]

6 Nena: "E, inu Ayuda! Ngati mwadziganizira kuti ndithu ndinu okondedwa a Allah kuposa (mitundu ina ya) anthu, ilakelakeni imfa (kuti mukalowe ku mtendere wa Allah) ngati mukunena zoona.
[Nena iwe Mtumiki (SAW) kwa anthu amene agwiritsa chipembedzo chowonengeka cha Chiyuda kuti: "Ngati mukudzigunda pa mtima – bodza- kutidi ndinu okondeka a Allah osati anthu ena amene sali mwa inu, ndiyetu ilakelakeni imfa ngati mukunena zoona podzitcha kwanu koti chikondi cha Allah ndi chanu.]

7 Ndipo sangailakelake mpang'ono pomwe chifukwa cha (zoipa) zimene manja awo atsogoza Allah akudziwa bwino za (anthu) opondereza.
[Ndipo Ayuda amenewa sangailakelake imfa mpaka kalekale chifukwa chosankha kukhala ndi moyo wa dziko lapansi kuposa moyo wa Tsiku Lomaliza, komanso kuopa chilango cha Allah pa iwo chifukwa cha zomwe adatsogoza zokanira Allah ndi ntchito zoipa. Palibe chingabisike kwa Iye mu kupondereza kwawo china chilichonse.]

8 Nena (kuti): "Ndithu imfa imene mukuithawa (palibe chikaiko) ikumana nanu; kenako mudzabwezedwa kwa Wodziwa zobisika ndi zooneka ndipo adzakuuzani zimene mudali kuchita.
[Nena: "Ndithu imfa imene mukuithawayi, palibe kwina kothawira ndithu iyo ikufikani panthawi yokwana nyengo yanu yofera kenako mudzabwezedwa Tsiku Lakiyama kwa Allah Wodziwa zimene zabisika ndi zomwe zaonekera ndipo adzakuwuzani za ntchito zanu zonse ndi kukulipirani pa zimenezo].

9 E, inu amene mwakhululupirira! Kukaitanidwa ku Swalaat Tsiku la Jum'a, pitani mwachangu kukamtamanda Allah, ndipo siyani malonda; zimenezo n''zabwino kwa inu ngati mukudziwa.
[E, inu amene mudamuvomera Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndi kutsatira malamulo Ake! Woitana akaitanira ku Swalaat Tsiku la Jum'a, pitani mwachangu kukamvera ulaliki komanso

يَٰٓأَيُّهَا ٱلَّذِينَ ءَامَنُوٓاْ إِذَا نُودِىَ لِلصَّلَوٰةِ مِن يَوْمِ ٱلْجُمُعَةِ
فَٱسْعَوْاْ إِلَىٰ ذِكْرِ ٱللَّهِ وَذَرُواْ ٱلْبَيْعَ ۚ ذَٰلِكُمْ خَيْرٌ لَّكُمْ إِن كُنتُمْ
تَعْلَمُونَ ﴿٩﴾ فَإِذَا قُضِيَتِ ٱلصَّلَوٰةُ فَٱنتَشِرُواْ فِى ٱلْأَرْضِ
وَٱبْتَغُواْ مِن فَضْلِ ٱللَّهِ وَٱذْكُرُواْ ٱللَّهَ كَثِيرًا لَّعَلَّكُمْ تُفْلِحُونَ
﴿١٠﴾ وَإِذَا رَأَوْاْ تِجَٰرَةً أَوْ لَهْوًا ٱنفَضُّوٓاْ إِلَيْهَا وَتَرَكُوكَ قَآئِمًا ۚ قُلْ
مَا عِندَ ٱللَّهِ خَيْرٌ مِّنَ ٱللَّهْوِ وَمِنَ ٱلتِّجَٰرَةِ ۚ وَٱللَّهُ خَيْرُ ٱلرَّٰزِقِينَ ﴿١١﴾

ترتيبها ٦٣ — سُورَةُ ٱلْمُنَافِقُونَ — آياتها ١١

بِسْمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحْمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

إِذَا جَآءَكَ ٱلْمُنَٰفِقُونَ قَالُواْ نَشْهَدُ إِنَّكَ لَرَسُولُ ٱللَّهِ ۗ وَٱللَّهُ يَعْلَمُ
إِنَّكَ لَرَسُولُهُۥ وَٱللَّهُ يَشْهَدُ إِنَّ ٱلْمُنَٰفِقِينَ لَكَٰذِبُونَ ﴿١﴾
ٱتَّخَذُوٓاْ أَيْمَٰنَهُمْ جُنَّةً فَصَدُّواْ عَن سَبِيلِ ٱللَّهِ ۚ إِنَّهُمْ سَآءَ مَا كَانُواْ
يَعْمَلُونَ ﴿٢﴾ ذَٰلِكَ بِأَنَّهُمْ ءَامَنُواْ ثُمَّ كَفَرُواْ فَطُبِعَ عَلَىٰ قُلُوبِهِمْ
فَهُمْ لَا يَفْقَهُونَ ﴿٣﴾ ۞ وَإِذَا رَأَيْتَهُمْ تُعْجِبُكَ أَجْسَامُهُمْ ۖ
وَإِن يَقُولُواْ تَسْمَعْ لِقَوْلِهِمْ ۖ كَأَنَّهُمْ خُشُبٌ مُّسَنَّدَةٌ ۖ يَحْسَبُونَ كُلَّ
صَيْحَةٍ عَلَيْهِمْ ۚ هُمُ ٱلْعَدُوُّ فَٱحْذَرْهُمْ ۚ قَٰتَلَهُمُ ٱللَّهُ ۖ أَنَّىٰ يُؤْفَكُونَ ﴿٤﴾

kukapemphera ndipo siyani kugulitsa komanso kugula (malonda aliwonse) komansno china chilichonse chimene chingakutangwanitseni ku Swalaatyo. Zimene mwalamulidwazi ndi zabwino kwa inu chifukwa muli kukhululukidwa machimo anu ndi malipiro a Allah, ngatidi mukuzindikira zokomera inu eni akenu, chitani zimenezi. Mu Ayat imeneyi muli umboni woti pali chikakamizo kupita kukapemphera Swalaat ya Jum'a ndikukamvera ulaliki (khutbah).]

10 Tsono Swalaat ikatha, balalikanani pa dziko ndipo funanifunani zabwino za Allah komanso m'tamandeni Allah kwambiri kuti mupambane (pa dziko lapansi komanso Tsiku Lomaliza).

[Ndipo mukatha kumvera ulaliki (khutbah) ndi kupemphera, ndiye balalikanani pa dziko ndikufunafuna rizq la Allah kudzera mu ntchito zanu. Ndipo mukumbukireni kwambiri Allah mu zinthu zanu zonse m'mene mulili kuti mupambane popeza zabwino za pa dziko lapansi komanso Tsiku Lomaliza.]

11 Ndipo akaona malonda kapena masewero, akubalalika kunka ku zimenezo ndi kukusiya uli chiimire (ukuchita khutbah ndi anthu ochepa). Nena (kwa iwo): "Zimene zili kwa Allah n"zabwino kwa inu kuposa masewero ndi malonda. Ndipo Allah Ngwabwino kwambiri popatsa (zopatsa) kuposa onse opatsa.

[Asilamu ena akaona malonda kapena kanthu kena kake mu za masewera za pa dziko ndi zokongoletsa zake,akubalalika kunka ku izo nkukusiya iwe Mtumiki (SAW) uli pa membari (gome) ukulalikira. Yankhula kwa iwo kuti: "Zomwe zili kwa Allah mu malipiro komanso mtendere ndi zothandiza kwambiri kwa inu kuposa masewero komanso malonda. Ndipo Allah Yekhayo ndiye wabwino kwambiri amene akupereka rizq ndi kupatsa, choncho pemphani kwa Iye. Ndipo dzithandizeni kudzera mkukumvera Iye popeza zimene zili kwa Iye ndi zabwino za pa dziko lapansi komanso Tsiku Lomaliza.]

## (63) SURATUL MUNAAFIQUN

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Akakudzera achipahamaso akunena kuti: "Tikuikira umboni kuti iwe ndiwe Mtumiki wa Allah," ndipo Allah akudziwa kuti iwe ndi Mtumiki Wake ndipo Allah akuikira umboni kuti achiphamaso ngabodza (pa zomwe akunena).

[Iwe Mtumiki (SAW), achipahamaso akadza pa malo ako azinena ndi malirime awo kuti: "Tikuikira umboni kuti iwe ndi mtumikidi wa Allah," ndipo Allah akudziwa kuti ndithudi iwe ndi Mtumiki wa Allah, ndipo Allah akuikira umboni kuti achiphamaso ndi abodza komanso zimene akuzionetsera za umboni wawo pa iwe komanso zimene alumbirirazo ndi malirime awo ndi kubisa ukafiri.]

2 Kulumbira kwawo (kwa bodza) akuchita kukhala chodzitetezera (chuma chawo ndi matupi awo). Ndipo akuletsa anthu (kuyenda) pa njira ya Allah. Ndithu n'zoipa zedi zimene amachita.

3 Zimenezo n'chifukwa chakuti iwo adakhulupirira (modzionetsera), kenako adakana (mobisa); choncho mitima yawo idatsekedwa, kotero kuti iwo sangathe kuzindikira (chimene chingawapulumutse ku chilango cha Allah).

[2&3: Ndithu achiphamaso achichita chikhulupiriro chawo chimene adalumbirira kukhala chodzitetezera ndi chotchingira chawo kuti asalangidwe. Kotero adzitsekereza okha komanso anthu ena ku njira yowongoka ya Allah. Ndithudi n'zoipa zedi zimene adali kuchita. Zimenezo n'chifukwa choti iwowo adakhulupirira mowonetsera kenako nakanira mwakabisibisi chifukwa cha ukafiri wawo, Allah adatseka mitima yawo kotero sangazindikirenso zinthu zomwe mkati mwake muli zabwino zawo.]

وَإِذَا قِيلَ لَهُمْ تَعَالَوْا۟ يَسْتَغْفِرْ لَكُمْ رَسُولُ ٱللَّهِ لَوَّوْا۟ رُءُوسَهُمْ
وَرَأَيْتَهُمْ يَصُدُّونَ وَهُم مُّسْتَكْبِرُونَ ﴿٥﴾ سَوَآءٌ عَلَيْهِمْ
أَسْتَغْفَرْتَ لَهُمْ أَمْ لَمْ تَسْتَغْفِرْ لَهُمْ لَن يَغْفِرَ ٱللَّهُ لَهُمْ ۚ إِنَّ
ٱللَّهَ لَا يَهْدِى ٱلْقَوْمَ ٱلْفَٰسِقِينَ ﴿٦﴾ هُمُ ٱلَّذِينَ يَقُولُونَ
لَا تُنفِقُوا۟ عَلَىٰ مَنْ عِندَ رَسُولِ ٱللَّهِ حَتَّىٰ يَنفَضُّوا۟ ۗ وَلِلَّهِ
خَزَآئِنُ ٱلسَّمَٰوَٰتِ وَٱلْأَرْضِ وَلَٰكِنَّ ٱلْمُنَٰفِقِينَ لَا يَفْقَهُونَ
﴿٧﴾ يَقُولُونَ لَئِن رَّجَعْنَآ إِلَى ٱلْمَدِينَةِ لَيُخْرِجَنَّ ٱلْأَعَزُّ
مِنْهَا ٱلْأَذَلَّ ۚ وَلِلَّهِ ٱلْعِزَّةُ وَلِرَسُولِهِۦ وَلِلْمُؤْمِنِينَ وَلَٰكِنَّ
ٱلْمُنَٰفِقِينَ لَا يَعْلَمُونَ ﴿٨﴾ يَٰٓأَيُّهَا ٱلَّذِينَ ءَامَنُوا۟ لَا تُلْهِكُمْ
أَمْوَٰلُكُمْ وَلَآ أَوْلَٰدُكُمْ عَن ذِكْرِ ٱللَّهِ ۚ وَمَن يَفْعَلْ
ذَٰلِكَ فَأُو۟لَٰٓئِكَ هُمُ ٱلْخَٰسِرُونَ ﴿٩﴾ وَأَنفِقُوا۟ مِن مَّا رَزَقْنَٰكُم
مِّن قَبْلِ أَن يَأْتِىَ أَحَدَكُمُ ٱلْمَوْتُ فَيَقُولَ رَبِّ لَوْلَآ أَخَّرْتَنِىٓ
إِلَىٰٓ أَجَلٍ قَرِيبٍ فَأَصَّدَّقَ وَأَكُن مِّنَ ٱلصَّٰلِحِينَ ﴿١٠﴾ وَلَن
يُؤَخِّرَ ٱللَّهُ نَفْسًا إِذَا جَآءَ أَجَلُهَا ۚ وَٱللَّهُ خَبِيرٌۢ بِمَا تَعْمَلُونَ ﴿١١﴾

ترتيبها ٦٤ — سُورَةُ التَّغَابُنِ — آياتها ١٨

(4) Ndipo ukawaona, akukondweretsa (kukula kwa) matupi awo, ndipo akayankhula, umvetsera zoyankhula zawo (chifukwa chakuthwa kwa malirime awo, pomwe mkati mwawo ndi mng'oma wopanda kanthu); iwo ali ngati matabwa womwe wayadzamiritsidwa ku chipupa (mwa iwo mulibe moyo). Mkuwo uliwonse (umene akuwumva) akuganiza kuti ukulinga iwo (chifukwa chakuzindikira chinyengo chawo); iwowa ndi adani, chenjerani nawo. Allah awatemberere! Mwa njira yanji akuchotsedwa ku (choonadi)!

[Ukawayang'ana achiphamasowa, akukondweretsa matupi awo ndi maonekedwe awo, ndipo akayankhula umvetsera zokamba zawo chifukwa chakuthwa kwa malirime awo kumachita kuti mitima yawo ilibe chikhulupiriro. Ndipo kupanda nzeru kwawo pakumvetsa zinthu ndi kuzindikira kothandiza, ali ngati matabwa amene ayedzamiritsidwa ku chipupa, amene mulibe moyo mkati mwake. Akumaganiza kuti mawu aliwonse wokwera, akugwera iwo komanso owasautsa iwo chifukwa chozindikira uchenicheni wawo ndi kupyola muyeso kwa mbali yawo, komanso mantha amene amanga nthenje pa mitima yawo. Iwowo ndi adani enieneni amene ali ndi upandu waukulu kwa iwe (Mtumiki SAW) komanso anthu okhulupirira choncho asamale. Allah awayalutsa ndiponso awapirikitsa ku chifundo Chake. Mwa njira yanji akuchotsedwa ku choonadi ndi kukakhala m'mene alilimo mu uchiphamaso ndi kusokera?]

(5) Kukanenedwa kwa iwo kuti : "Bwerani akupemphereni chikhululuko Mtumiki wa Allah (SAW)", akutembenuza mitu yawo (monyoza ndi modzitukumula), ndipo uwaona akunyoza uku akudzikweza (osatsatira langizo)

[Kutati kunenedwe kwa achiphamasowa kuti: "Tabwererani uku mukulapa ndi kupepesa zomwe zidachoka kwa inu mu zoyankhula zachabe ndi nkhani zopusa, Mtumiki (SAW) akupempherani chikhululuko ndi kumupempha Allah kuti akukhululukireni ndi kukufafanizirani machimo anu", iwo akupendeketsa mitu yawo ndi kuigwedeza mwa chipongwe ndi kudzikweza. Ndipo uwaona iwowo iwe Mtumiki (SAW) akuyang'ana kumbali kwa iwe uku akudzikuza kusiya kutsatira zomwe zafunikira kuchokera kwa iwo.]

(6) Kwa iwowa n'chimodzimodzi kuwapemphera kwako chikhululuko, kapena kusawapemphera, Allah sadzawakhululukira (chifukwa chakuzama kwawo mu ukafiri), ndithu Allah saongola anthu otuluka m'chilamulo Chake.

[Ndi chimodzimodzi kwa achiphamaso amenewa utati iwe Mtumiki (SAW) uwapemphere chikhululuko kwa Allah kapena ayi , ndithu Allah sadzakhululuka machimo awo mpaka muyaya, chifukwa chopitiriza kwawo kukhala oipitsitsa ndi kukhazikika kwawo mu ukafiri. Ndithu Allah sawapatsa chisomo cha chikhulupiriro anthu amene akumukana Iye, opandukira ulamuliro Wake.]

(7) Amenewa ndiwo omwe akunena (kwa Answaari – Asilamu a ku Madina, kuti): "Musawapatse chuma (chanu) amene ali ndi Mtumiki wa Allah (SAW) kuti abalalikane". Pomwe chuma chonse cha kumwamba ndi cha dziko lapansi chili m'manja mwa Allah (ndipo amachipereka kwa amene wam'funa); koma achiphamaso sakuzindikira (zimenezo).

[Achiphamaso amenewa ndi amene akumanena kwa Asilamu a pa Madina kuti: "Musapatse chuma ophunzira a Mtumiki wa Allah (SAW) osamuka kuchokera ku Makka kufikira atabalalikana kumusiya iyeyo (SAW). Ndipo nkhokwe zonse za chuma cha kumwamba ndi pa dziko lapansi komanso zili m'menemo mu

marizq, ndi za Allah Yekha amam'patsa amene wam'funa ndikumumana amenenso wam'funa. Koma achiphamasowa alibe kuzindikira ndipo sizingathandize zimenezo.]

(8) Akunena kuti : "Ngati tibwerera ku Madina, wolemekezeka adzatulutsa wonyozeka m'menemo". Pomwe ulemerero ngwa Allah ndi Mtumiki wake (SAW) ndi okhulupirira, koma achiphamaso sakudziwa (zimenezo).

[Achiphamaso amenewa akunena kuti: "Ngati titabwerera ku Madina ndithudi gulu lathu lolemekezeka likatulutsa mu mzindawu gulu la okhulupirira onyozeka". Komatu ulemerero onse ndi wa Allah, Mtumiki wake (SAW) komanso anthu okhulupirira mwa Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) osati ena aliwonsewo osakhala iwo, koma achiphamaso sakuzindikira zimenezo chifukwa cha umbuli wawo wopyola malire.

(9) E, inu amene mwakhulupirira! Kuika mtima pa chuma chanu ndi ana kusakuchiteni kuti mukhale wotanganidwa ndi kusiya kumukumbukira Allah (ndi kukwaniritsa zimene wakulamulani). Ndipo amene achite zimenezo iwowo ndi otaika.

[E, inu amene mudamuvomereza Allah, Mtumiki Wake (SAW) ndi kugwiritsa ntchito malamulo Ake! Chuma chanu komanso ana anu asakutangwanitseni kusiya kumpembedza Allah ndi kumumvera. Amene chuma chake ndi ana angamutangwanitse kusiya zomenezo, ndiye ndi otaya mwayi wawo ku ulemerero wa Allah ndi chifundo Chake.]

(10) Perekani mwachangu (pa njira ya Allah) zina mwa zomwe takupatsani, isanam'fikire m'modzi wa inu imfa (mwadzidzidzi) ndi kuyamba kunena (modandaula): "Mbuye wanga! Bwanji wosandichedwetsa nthawi pang'ono kuti ndipereke sadaka (ndi kuti ndikonze zina zimene sindinazikwaniritse) ndi kuitinso ndikhale mwa anthu abwino".

[Ndipo inu amene mwakhulupirira mwa Allah ndi Mtumiki Wake (SAW), perekani mwa zina zimene takupatsani mu njira ya zabwino. Fulumizitsani zimenezi isadam'fike m'modzi wa inu imfa ndikuona zisonyezo zake ndi zizizndikiro za imfayo nkudzanena modandaula kuti: "Mbuye wanga! Bwanji wosandichedwetsako ndi kuidikira imfa yanga kufikira kanthawi kena kakafupi n'cholinga choti ndikaperekeko chopereka cha chuma changa ndikuti nkakhale mwa anthu ochita zabwino owopa.]

(11) Ndipo Allah sauchedwetsa mzimu (ngakhale ndi mphindi imodzi) ukaidzera nthawi yake ya imfa; ndipo Allah Ngodziwa zonse zimene mukuchita (ndipo adzakulipirani pa zimenezo).

[Ndipo Allah sadzauchedwetsa mzimu uli wonse ikafika nthawi ya imfa yake ndi kutha moyo wake. Ndipo Allah Subhaanahu ndi Wozindikira zinthu zimene inu mukuzichita mu zabwino kapena zoipa, kotero adzakulipirani nazo.]

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَٰنِ الرَّحِيمِ

يُسَبِّحُ لِلَّهِ مَا فِي السَّمَاوَاتِ وَمَا فِي الْأَرْضِ ۖ لَهُ الْمُلْكُ وَلَهُ الْحَمْدُ ۖ
وَهُوَ عَلَىٰ كُلِّ شَيْءٍ قَدِيرٌ ١ هُوَ الَّذِي خَلَقَكُمْ فَمِنكُمْ كَافِرٌ
وَمِنكُم مُّؤْمِنٌ ۚ وَاللَّهُ بِمَا تَعْمَلُونَ بَصِيرٌ ٢ خَلَقَ السَّمَاوَاتِ
وَالْأَرْضَ بِالْحَقِّ وَصَوَّرَكُمْ فَأَحْسَنَ صُوَرَكُمْ ۖ وَإِلَيْهِ الْمَصِيرُ ٣
يَعْلَمُ مَا فِي السَّمَاوَاتِ وَالْأَرْضِ وَيَعْلَمُ مَا تُسِرُّونَ وَمَا تُعْلِنُونَ ۚ وَاللَّهُ
عَلِيمٌ بِذَاتِ الصُّدُورِ ٤ أَلَمْ يَأْتِكُمْ نَبَأُ الَّذِينَ كَفَرُوا مِن قَبْلُ
فَذَاقُوا وَبَالَ أَمْرِهِمْ وَلَهُمْ عَذَابٌ أَلِيمٌ ٥ ذَٰلِكَ بِأَنَّهُ كَانَت تَّأْتِيهِمْ
رُسُلُهُم بِالْبَيِّنَاتِ فَقَالُوا أَبَشَرٌ يَهْدُونَنَا فَكَفَرُوا وَتَوَلَّوا ۚ وَّاسْتَغْنَى
اللَّهُ ۚ وَاللَّهُ غَنِيٌّ حَمِيدٌ ٦ زَعَمَ الَّذِينَ كَفَرُوا أَن لَّن يُبْعَثُوا ۚ قُلْ بَلَىٰ وَرَبِّي
لَتُبْعَثُنَّ ثُمَّ لَتُنَبَّؤُنَّ بِمَا عَمِلْتُمْ ۚ وَذَٰلِكَ عَلَى اللَّهِ يَسِيرٌ ٧ فَآمِنُوا بِاللَّهِ
وَرَسُولِهِ وَالنُّورِ الَّذِي أَنزَلْنَا ۚ وَاللَّهُ بِمَا تَعْمَلُونَ خَبِيرٌ ٨ يَوْمَ
يَجْمَعُكُمْ لِيَوْمِ الْجَمْعِ ۖ ذَٰلِكَ يَوْمُ التَّغَابُنِ ۗ وَمَن يُؤْمِن بِاللَّهِ وَيَعْمَلْ
صَالِحًا يُكَفِّرْ عَنْهُ سَيِّئَاتِهِ وَيُدْخِلْهُ جَنَّاتٍ تَجْرِي مِن تَحْتِهَا
الْأَنْهَارُ خَالِدِينَ فِيهَا أَبَدًا ۚ ذَٰلِكَ الْفَوْزُ الْعَظِيمُ ٩

## (64) SURAT TAGHAABUN

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Zonse za kumwamba ndi za m'dziko lapansi zikulemekeza Allah ndi kum'patula ku zinthu zosayenerana ndi ulemerero Wake. Ufumu Ngwake, ndipo kutamandidwa kwabwino N'kwake. Iye ali ndi kuthekera pa chilichonse.

[Zimamuyeretsa Allah ku zinthu zina zili zonse zosayenerana ndi Iye, zonse zimene zili kumwamba komanso pa dziko lapansi. Iye ali nacho chifuniro chonse

(2) Iye ndi Amene adakulengani (nonsenu popanda kuchokera pa chilichonse) choncho mwa inu alipo wokhulupirira. Ndipo Allah Ngopenya zonse zimene mukuchita (ndipo adzakulipirani nazo).[Allah ndi Amene adachititsa kuti inuyo mupezeke kuchokera

mosakhala kalikonse. Ndipo ena a inu akukanira umulungu Wake pamene ena akuvomereza zimenezo nkumagwiritsira ntchito malamulo Ake. Iye Subhaanahu Ngoyang'ana ntchito zanu palibe chobisika kwa Iye mu zimenezo ndipo adzakulipirani nazo.]

(3) Adalenga thambo ndi nthaka mwachoonadi, ndipo adakujambulani majambulidwe abwino; ndipo kobwerera nkwa Iye (pa Tsiku Lomaliza). [Allah adalenga thambo ndi nthaka mwa nzeru zakuya zedi ndipo adakulengani mu maonekedwe abwino kwambiri. Kwa Iye ndiko kobwerera Tsiku Lakiyama ndipo adzalipira aliyense ndi ntchito zake].

(4) (Allah) akudziwa za kumwamba ndi za m'dziko la pansi, ndiponso akudziwa zimene mukuzibisa ndi zimene mukuzilengeza (zochita ndi zoyankhula); Allah Ngodziwa zimene ziri m'zifuwa.[Subhaanahu Wataalaa akudziwa chili chonse cha kumwamba komanso pa dziko lapansi, komanso akudziwa zimene inu anthu mukubisa pakati panu ndinso zimene mukuonetsera. Allah akudziwa zimene zifuwa zikusunga ndi zimene mitima ikuzibisa.]

(5) Kodi siidakufikeni nkhani ya omwe sadakhulipirire kale? Adalawa (zowawa) za zoipa za zinthu zawo (pa dziko lapansi) ndipo chilango chowawa chidzakhala pa iwo (Tsiku Lomaliza).[Kodi inu opembedza mafano (amushrikina), siidakufikeni nkhani ya anthu amene adakanira mu magulu amene adamuka pa tsogolo panu; pamene kudawapeza kuipa kwa mapeto a ukafiri wawo ndi kuipa kwa zochita zawo pa dziko lapansi, ndipo ali nacho chilango chowawa molapitsa Tsiku Lomaloza?]

(6) Zimenezo n'chifukwa chakuti Atumiki awo amawadzera ndi zozwizwitsa koma iwo amanena (mwachipongwe) "Ha! Anthu anzathu (onga ife) angationgole?" Choncho sadakhulupirire (utumiki wawo) ndipo adanyoza (choonadi) potero Allah adawasiya (ndi kupanda chikhulupiriro kwawo) Allah Ngokwanira ndiponso Ngoyamikidwa.[Zimene zidawapezazo pa dziko la pansi ndi zomwe zidzawapeze Tsiku Lomaliza, chifukwa choti ndithu iwo ankati akawadzera Atumiki a Allah ndi zizindikiro zowonekera komanso zozwizwitsa ankanena mokanitsitsa kuti: "Kodi anthu onga ife tomwe nkutiongolera? Kotero adakanira Allah komanso utumiki wa Atumiki Ake ndi kutalikira ku choonadi ndipo sadachilandire. Ndiye Allah adadzikwaniritsa ndipo Allah Ngwachikwanekwane. Ali nawo uchikwanekwane wopanda malire, Woyamikidwa mu zoyankhula Zake komanso zochita Zake kudzanso mbiri Zake, salabadira za iwo, ndipo **kusokera** kwawo sikungamusautse kalikonse.]

(7) Amene sadakhulupirire akumanama kuti sadzaukitsidwa ku imfa. Nena (kwa iwo iwe Muhammad SAW, sizili choncho monga mukunenera): "Pali Mbuye wanga, ndithu mudzaukitsudwa ku imfa ndipo mudzauzidwa zimene mumachita (pa dziko lapansi). Zimenezo kwa Allah n'zosavuta.[Anthu okanira Allah akumanama mwabodza kuti ndithu iwo sadzatulutsidwa m'manda mwawo pambuyo pa imfa, nena kwa iwo iwe Mtumiki (SAW): "Mtheradi pali Mbuye wanga, ndithudi inu mudzatulutsidwa kuchokera m'manda mwanu muli amoyonso, kenako mudzauzidwadi zimene mudachita pa dziko lapansi ndipo zimenezo kwa Allah n'zofewa kuzichita.]

(8) Khulupirirani Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndi dangalira limene talivumbulutsa. Ndipo Allah Ngodziwa kwambiri zimene mukuchita.[Ndiye inu amushrikina khulupirirani mwa Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndipo wongokani ndi Qur'aan imene adaivumbulutsa kwa Mtumiki Wake (SAW). Ndipo Allah Ngozindikira, palibe chilichonse chimene chingabisike kwa Iye mu ntchito zanu komanso zoyankhula zanu.]

(9) (Kumbukirani) tsiku limene adzakusonkhanitseni chifukwa cha Tsiku Lakusonkhana (zolengedwa zonse), limenelo ndi tsiku lolephera(akafiri adzakhala olephera chifukwa cha kusakhulupirira kwawo. Nawo Asilamu aulesi adzakhla olephera chifukwa cha kusakwaniritsa kwawo malamulo a Allah). Ndipo amene akhulupirira mwa Allah ndi kuchita zabwino, am'fafanizira zoipa zake ndipo akamulowetsa m'minda momwe pansi pake pakuyenda mitsinje; adzakhala m'menemo muyaya. Kumeneko ndiko kupambana kwakukulu. [Inu likumbukireni tsiku losonkhanitsa limene Allah adzasonkhanitse anthu oyambirira komanso omalizira. Tsiku limenelo ndilo mudzaonekemo kulephera ndi kusiyana pakati pa zolengedwa. Anthu okhulupirira adzawalepheretsa ndi kuwapambana makafiri ndi anthu oipitsitsa, ndipo anthu a chikhulupiriro akalowa ku jannat kudzera mu chisomo cha Allah, ndipo eni ukafiri akalowa ku moto kudzera mu chilungamo cha Allah. Amene akhulupirire ndikugwira ntchito zomvera Iye, amufafanizira machimo ake nkukamulowetsa m'minda imene pansi pa nyumba zawo zachifumu pakuyenda mitsinje. Akakhala m'menemo muyaya. Kukhala muyayako m'mindayo,

وَٱلَّذِينَ كَفَرُواْ وَكَذَّبُواْ بِـَٔايَٰتِنَآ أُوْلَٰٓئِكَ أَصۡحَٰبُ
ٱلنَّارِ خَٰلِدِينَ فِيهَاۖ وَبِئۡسَ ٱلۡمَصِيرُ ١٠ مَآ أَصَابَ مِن
مُّصِيبَةٍ إِلَّا بِإِذۡنِ ٱللَّهِۗ وَمَن يُؤۡمِنۢ بِٱللَّهِ يَهۡدِ قَلۡبَهُۥۚ وَٱللَّهُ بِكُلِّ
شَيۡءٍ عَلِيمٞ ١١ وَأَطِيعُواْ ٱللَّهَ وَأَطِيعُواْ ٱلرَّسُولَۚ فَإِن
تَوَلَّيۡتُمۡ فَإِنَّمَا عَلَىٰ رَسُولِنَا ٱلۡبَلَٰغُ ٱلۡمُبِينُ ١٢ ٱللَّهُ لَآ إِلَٰهَ
إِلَّا هُوَۚ وَعَلَى ٱللَّهِ فَلۡيَتَوَكَّلِ ٱلۡمُؤۡمِنُونَ ١٣ يَٰٓأَيُّهَا
ٱلَّذِينَ ءَامَنُوٓاْ إِنَّ مِنۡ أَزۡوَٰجِكُمۡ وَأَوۡلَٰدِكُمۡ عَدُوّٗا
لَّكُمۡ فَٱحۡذَرُوهُمۡۚ وَإِن تَعۡفُواْ وَتَصۡفَحُواْ وَتَغۡفِرُواْ
فَإِنَّ ٱللَّهَ غَفُورٞ رَّحِيمٌ ١٤ إِنَّمَآ أَمۡوَٰلُكُمۡ وَأَوۡلَٰدُكُمۡ
فِتۡنَةٞۚ وَٱللَّهُ عِندَهُۥٓ أَجۡرٌ عَظِيمٞ ١٥ فَٱتَّقُواْ ٱللَّهَ مَا ٱسۡتَطَعۡتُمۡ
وَٱسۡمَعُواْ وَأَطِيعُواْ وَأَنفِقُواْ خَيۡرٗا لِّأَنفُسِكُمۡۗ وَمَن
يُوقَ شُحَّ نَفۡسِهِۦ فَأُوْلَٰٓئِكَ هُمُ ٱلۡمُفۡلِحُونَ ١٦ إِن تُقۡرِضُواْ
ٱللَّهَ قَرۡضًا حَسَنٗا يُضَٰعِفۡهُ لَكُمۡ وَيَغۡفِرۡ لَكُمۡۚ وَٱللَّهُ شَكُورٌ
حَلِيمٌ ١٧ عَٰلِمُ ٱلۡغَيۡبِ وَٱلشَّهَٰدَةِ ٱلۡعَزِيزُ ٱلۡحَكِيمُ ١٨

ترتيبها ٦٥ — سُورَةُ الطَّلَاقِ — آياتها ١٢

kumeneko ndiko kupambana kwakukulu palibenso kupambana kwina pambuyo pake.]

(10) Koma amene sadakhulupirire natsutsa zozwizwitsa Zathu (zimene zidaperekedwa kwa aneneri Athu), iwowo ndi anthu a ku moto, adzakhala m'menemo muyaya, amenewo ndiwo mabwerero woipa.

[Ndipo anthu amene adakana zoti ndithu Allah ndi amene ali wopembedzedwa mwachoonadi ndipo nakaniranso zisonyezo za umbuye Wake ndi maumboni a kuyenerera kopembedzedwa Iye yekhayo omwe adawatumiza nawo atumiki Ake, iwowo ndi eni moto ndipo akakhalamo muyaya. Ndipo aipa mabwerero amene iwo adzakhalemo amene ali jahannama (jahena).]

(11) Palibe vuto lililonse lingapezeke pokhapokha Allah atafuna. Ndipo amene akhulupirira Allah, (Allah) awongola mtima wake (kuti ukhale wokhutira ndi chiweruzo cha Allah). Ndipo Allah Ngodziwa chinthu chilichonse.

[Palibe chimene chingampeze wina aliyense mwa sautso pokhapokha chimam'peza mwa chilolezo cha Allah komanso chigamulo Chake kudzanso chiringanizo Chake. Ndipo amene akhulupirire mwa Allah, Iyeyo awongolera mtima wake kuti udzizipereka ku lamulo Lake ndi kukhuthira ndi chigamulo Chake ndikumuongoleranso ku zoyankhula ndi zochitanso zabwino ndinso makhalidwe abwino chifukwa tsinde la chiongolo umakhala mtima pamene ziwalo zimangotsatira. Ndipo Allah ndi wodziwa chinthu chilichonse palibe chingabisike kwa Iye mwa izo.]

(12) Choncho mverani Allah ndipo mverani Mtumiki (SAW). Ngati munyozere (ndi zanu), udindo wa Mtumiku Wathu (SAW) ndi kufikitsa uthenga basi momveka ndi mowonekera.

[Choncho inu anthu mverani Allah ndipo muwongokere kwa Iye pa zimene walamula ndi zomwe waziletsa, ndipo mvereni Mtumiki (SAW) mu zomwe wazifikitsa kwa inu zochokera kwa Mbuye wake. Ngati muti monyozere, n'kusiya kumvera Allah ndi Mtumiki Wake (SAW), ndiyetu palibe vuto lili lonse kwa Mtumiki Wathu (SAW) pa kunyozera kwanuko. Ndthudi zomwre zakakamizidwa pa iye (SAW) ndiko kukufikitsirani zomwe watumizidwa nazo kufikitsa koonekera.]

(13) Allah, palibe wina wopembedzedwa mwachoonadi koma Iye. Ndipo kwa Allah Yekha, okhulupirira atsamire. [Allah, yekhayo, palibe wopembedzedwa mwachoonadi kupatula Iye, ndipo pa Allah ayedzamire anthu okhulupirira za umodzi Wake mu zinthu zawo zonse.]

(14) E, inu amene mwakhulupirira!Ndithu ena mwa akazi anu ndi ana anu ndi adani anu (chifukwa chakuti amakuchotsani kumbali yomvera Allah pofuna kuti mukwaniritse zofuna zawo). Chenjerani nawo (apeweni). Ngati muwakhululukira ndi kunyalanyaza ndi kubisa zolakwa zawo ndi bwino kwambiri , ndithu Allah Ngokhululuka kwambiri, Ngwachifundo chambiri.[E, inu amene mwakhulupirira mwa Allah ndi Mtumiki Wake (SAW)! Ndithudi mwa akazi anu ndinso ana anu ndi adani anu akutsekereza ku njira ya Allah ndi kukupingani za kumumvera Iye choncho khalani tcheru ndi iwo ndipo musamawamvere. Ngati mutakhululuka zolakwa zawo ndi kusaziikira ku mtima komanso kuzibisa kwa iwowo, ndithudi Allah Ngokhululuka, Ngwachisoni, kotero akukhululukirani machimo anu chifukwa Iye Subhaanahu Ngwachichikhululuko chachikulu ndi chisoni chotambasuka].

(15) Ndithu, chuma chanu ndi ana anu ndi mayeso (kwa inu); koma kwa Allah kuli malipiro aakulu (kwa yemwe wasankha kumvera Allah). [Chuma chanu ndi ana anu sichina koma

mayesero kwa inu. Ndipo Allah ali nawo malipiro aakulu kwa amene wasankha kumvera Iye kuposa kumvera wina aliyense wosakhala Iye ndipo napereka zoyenerera kuchitira Allah mu chuma chake.]

16 Choncho muopeni Allah m'mene mungathere ndipo mverani (ziphunzitso Zake) ndipo tsatirani (malamulo Ake), perekani (zimene wakupatsani) zikhala zabwino kwa inu. Ndipo amene watchinjirizidwa ku umbombo wake, iwowo ndiwo opambana.

[Choncho inu amene mwakhulupirira chitirani khama ndi nkhongono zanu zonse pomuopa Allah ndipo mvereni Mtumiki wa Allah (SAW) kumumvera koganizira mozama komanso mverani malamulo Ake ndipo pewani zoletsedwa zake. Komanso perekani zimene Allah wakupatsani kutero kukhala kwabwino kwa inu. Ndipo amene wapulumuka ku umbombo ndi kumana zotsala za chuma, iwowo ndiwo opambana ndi zabwino zonse, komanso opambana popeza zonse zimene akuzifuna.]

17 Ngati mungam'kongoze Allah ngongole yabwino, ayiwonjezera kwa inu (malipiro ake) ndipo akukhululukirani, ndipo Allah Ngolandira kuthokoza, Ngoleza (ndipo sachita changu polanga).

[Ngati mutapereka chuma chanu mu njira ya Allah modziyeretsa ndi chisangalalo cha mtima, Allah achulukitsa malipiro a zomwe mwaperekazo komanso akukhululukirani machimo anu ndipo Allah Ngolandira kuthokoza kwa anthu opereka powapatsa malipiro abwino pa zomwe adapereka,Ngoleza moti safulumizitsa kulanga amenewamulakwira.]

18 Ngodziwa zobisika ndi zowonekera; Ngwamphamvu zopambana, Ngwanzeru zakuya.

[Iye Subhaanahu Ngodziwa chilichonse chimene chabisika ndi chimene chaonekera, Ngwamphamvu zoposa Amene sagonjetsedwa, Ngwanzeru zakuya mu zoyankhula ndi zochita Zake.]

## (65) SURAT ATALAQ

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ
يَٰٓأَيُّهَا ٱلنَّبِيُّ إِذَا طَلَّقۡتُمُ ٱلنِّسَآءَ فَطَلِّقُوهُنَّ لِعِدَّتِهِنَّ وَأَحۡصُواْ
ٱلۡعِدَّةَۖ وَٱتَّقُواْ ٱللَّهَ رَبَّكُمۡۖ لَا تُخۡرِجُوهُنَّ مِنۢ بُيُوتِهِنَّ
وَلَا يَخۡرُجۡنَ إِلَّآ أَن يَأۡتِينَ بِفَٰحِشَةٖ مُّبَيِّنَةٖۚ وَتِلۡكَ حُدُودُ
ٱللَّهِۚ وَمَن يَتَعَدَّ حُدُودَ ٱللَّهِ فَقَدۡ ظَلَمَ نَفۡسَهُۥۚ لَا تَدۡرِي لَعَلَّ
ٱللَّهَ يُحۡدِثُ بَعۡدَ ذَٰلِكَ أَمۡرٗا ١ فَإِذَا بَلَغۡنَ أَجَلَهُنَّ فَأَمۡسِكُوهُنَّ
بِمَعۡرُوفٍ أَوۡ فَارِقُوهُنَّ بِمَعۡرُوفٖ وَأَشۡهِدُواْ ذَوَيۡ عَدۡلٖ مِّنكُمۡ
وَأَقِيمُواْ ٱلشَّهَٰدَةَ لِلَّهِۚ ذَٰلِكُمۡ يُوعَظُ بِهِۦ مَن كَانَ يُؤۡمِنُ
بِٱللَّهِ وَٱلۡيَوۡمِ ٱلۡأٓخِرِۚ وَمَن يَتَّقِ ٱللَّهَ يَجۡعَل لَّهُۥ مَخۡرَجٗا ٢ وَيَرۡزُقۡهُ
مِنۡ حَيۡثُ لَا يَحۡتَسِبُۚ وَمَن يَتَوَكَّلۡ عَلَى ٱللَّهِ فَهُوَ حَسۡبُهُۥٓۚ إِنَّ ٱللَّهَ
بَٰلِغُ أَمۡرِهِۦۚ قَدۡ جَعَلَ ٱللَّهُ لِكُلِّ شَيۡءٖ قَدۡرٗا ٣ وَٱلَّٰٓـِٔي يَئِسۡنَ
مِنَ ٱلۡمَحِيضِ مِن نِّسَآئِكُمۡ إِنِ ٱرۡتَبۡتُمۡ فَعِدَّتُهُنَّ ثَلَٰثَةُ أَشۡهُرٖ
وَٱلَّٰٓـِٔي لَمۡ يَحِضۡنَۚ وَأُوْلَٰتُ ٱلۡأَحۡمَالِ أَجَلُهُنَّ أَن يَضَعۡنَ حَمۡلَهُنَّۚ
وَمَن يَتَّقِ ٱللَّهَ يَجۡعَل لَّهُۥ مِنۡ أَمۡرِهِۦ يُسۡرٗا ٤ ذَٰلِكَ أَمۡرُ ٱللَّهِ أَنزَلَهُۥٓ
إِلَيۡكُمۡۚ وَمَن يَتَّقِ ٱللَّهَ يُكَفِّرۡ عَنۡهُ سَيِّـَٔاتِهِۦ وَيُعۡظِمۡ لَهُۥٓ أَجۡرًا ٥

1 E, iwe Mneneri (SAW)! Ngati mufuna kusudzula akazi ukwati, asudzuleni m'nyengo yowerengera edda yawo (kuwerengera edda kumayambika mkazi akakhala ndi twahara akachira matenda a kumwezi). Ndipo werengerani nyengo ya edda. Muopeni Allah Mbuye wanu. Ndipo musawatulutse m'nyumba zawo komanso asatuluke kupatula atachita tchimo lalikulu lowonekera (loyenera chilango, apo atha kutulutsidwa). Ndipo amenewa ndiwo malire a Allah (amene awakhazikitsa kwa anthu Ake); ndipo amene apyole malire a Allah, wadzichitira yekha zoipa, siukudziwa (cholinga cha malamulo amenewa) mwina Allah adzadzetsa chinthu pambuyo pake (chosonyeza kuyanjana).

[E, iwe Mneneri (SAW)! Ukafuna iwe kapena anthu okhulupirira kuti musudzule akazi anu, asudzuleni pa nthawi imene akuchingamira kuyera kwawo – mu nthawi imene atangomaliza kudwala matenda a kumwezi ndipo simunakhale nawo malo amodzi, kapena mu nyengo yoti ali ndi pakati powonekera- ndipo sungani nyengo ya chidikiriro kuti mudziwe nthawi yowabwerera ngati mutafuna kutero. Ndipo muopeni Allah Mbuye wanu. Musatulutse akazi osudzulidwa m'nyumba zimene iwo akukhalamo kufikira itatha nthawi yachidikiriro yawo yomwe ndi kudwala matenda a kumwezi katatu kwa amene sali mwana wamng'ono, ntchembere youma ndi mzimayi woyembekezera. Ndipo nkosaloledwa kwa iwo kutuluka m'nyumbazo mwa iwo okha kupatula atachita chinthu choipitsitsa chowonekera monga chigololo. Amenewo ndiwo malamulo a Allah amene adawaikira akapolo Ake. Yemwe angapyole

malire (malamulo a Allah) ndiye kuti wadzipondereza yekha ndipo wadziika yekha pa chionongeko. Iwe wosudzulawe siukudziwa kuti mwina Allah angachititse kanthu kena kake kamene simumayembekezera pambuyo pa chisudzulocho nkudzabwererana nawo.]

(2) Ngati osiyidwawo nyengo yawo ya (edda) itayandikira kutha,abwerereni mwa ubwino kapena asiyeni mwa ubwino (polekerera nyengoyo kuti ithe). Ndipo (powabwerera) funani mboni ziwiri zolungama zochokera mwa inu (zimene zichitire umboni kuti inu mukubwererana), ndipo perekani umboni chifukwa choopa Allah. Zimenezo ndizo akulangizidwa nazo amene akhulupirira mwa Allah ndi Tsiku Lomaliza. Ndipo amene akumuopa Allah (potsatira malamulo Ake) am'konzera njira yotulukira (m'mavuto).

(3) Ndipo am'konzera njira zopezera riziq kuchokera momwe samayembekezeramo. Ndipo amene akutsamira kwa Allah (pa zinthu zake zonse), ndiye kuti Allah ali wokwana kwa iye (kum'konzera chilichonse). Ndithu Allah ngokwaniritsa cholinga Chake. Ndithu chinthu chilichonse Allah wachipatsa mlingo wake woyenera (ndipo sichingamupyole).

2,3 [Pamene akuyandikira mapeto a nyengo ya edda ya azimayi osiidwa, ndiye abwerereni ndikukhalirana nawo mwa ubwino popereka kwa iwo zosoweka zawo kapena siyanani nawo pamodzi ndi kukwaniritsa zowayenerera zawo (maufulu awo) popanda kuwasautsa. Achitire umboni pobwererapo kapena kusiyanako amuna awiri achilungamo ochokera mwa inu. Ndipo inu amene muli mboni perekani umboni woyenera chifukwa cha Allah osati kanthu kena kali konse ayi. Zimenezo ndi zimene wakulamulani, akulangizidwa nazo munthu amene akukhulupirira mwa Allah ndi Tsiku Lomaliza. Ndipo amene awope Allah nagwiritsira ntchito zimene wamulamula nazo, napewa zimene Iye wamuletsa kuzichita, amuchitira potulukira mu mavuto aliwonse. Ndiponso amufewertsera njira zopezera rizq kuchokera komwe iye samaganizira ndipo komwe samawerengera. Ndipo munthu amene ayedzamire mwa Allah, ndiyetu Iyeyo amukwanira mu chinthu chilichonse chom'patsa phuma mu zinthu zake zonse. Ndithu Allah ndi wokwaniritsa kuchita zinthu Zake ndipo palibe chimene chingamudutse komanso sichingamulepheretsa chinthu chofunika. Ndithudi Allah adaika pa chinthu chilichonse nyengo yotherapo ndiponso mulingo woti sangaudutse.]

(4) Ndipo edda ya amene asiya kudwala kumwezi mwa akazi anu (chifukwa chakukula) ngati mukaika (nthawi ya edda yawo), edda yawo ndi miyezi itatu. Ndi omwe sadathe msinkhu edda yawo ndi momwemonso. Tsono akazi apakati nthawi yothera edda yawo ndi pomwe abereka. Ndipo amene aopa Allah, am'fewetsera zinthu zake (kuti zikhale zosavuta). [Azimayi osudzulidwa amene matenda akumwezi adasiya chifukwa chokula msinkhu wawo, ngati mutakaikira ndipo simudadziwe chiweluzo pa iwo, ndiye kuti edda yawo miyezi itatu chimodzimodzinso atsikananso ang'onoang'ono amene sadayambe kudwala matendawa, edda yawo ndi miyezinso itatu. Tsono mwa azimayi apakati, edda yawo ndiko kubereka kwawo. Ndipo amene aope Allah nakwaniritsa malamulo Ake, amuchitira mu zinthu zake kukhala zofewa pano pa dziko lapansi komanso Tsiku Lomaliza.]

(5) Limenelo ndi lamulo la Allah (lomwe) walikhazikitsa kwa inu; ndipo amene aope Allah (posunga malamulo Ake) amamufafanizira zoipa zake, ndiponso amamukulitsira malipiro ake. [Izo zomwe zatchulidwa zokhudzana chisudzulo ndi edda ndi lamulo la Allah limene walitumiza kwa inu anthu kuti mudzirigwiritsira ntchito. Ndipo munthu amene aope Allah (moona mtima) potalikira kumunyoza ndi popanga malamulo Ake achikakamizo, amufutira machimo ake ndi kumuchulukitsira malipiro Tsiku Lomaliza ndi kukamulowetsa ku jannat.]

(6) Akhazikeni (osiidwawo) m'mene mukukhala inumo monga momwe kulili kupeza kwanu (ndi mphamvu zanu ngakhale kuti mwawasiya ukwati). Musawavute ndi cholinga chowapana (kuti athawe okha). Ngati ali ndi pakati, apatseni zonse zofunika pa moyo mpaka adzabereke. Ngati akukuyamwitsirani ana anu, apatseni malipiro awo mokwanira; gwirizanani pakati panu mwa ubwino ndi mofatsa. Ngati wina apereka mavuto kwa mnzake (ndiye kuti mwanayo) adzamuyamwitsira (mkazi) wina, osati osiyidwayo. [Akhazikeni akazi osiidwa mwa akazi anu mu nyengo ya edda yawo mofanana ndi kakhalidwe kanu mwa mulingo wa kapezedwe kanu ka zinthu ndi mphamvu zanu. Ndipo musawasautse kuti muwapane pokhala. Ngati akazi anu osiidwawo ndi apakati, ndiye mudziwapatsa zofunikira zawo pa nyengo ya edda yawo kufikira atabereka. Ngati atakuyamwitsirani ana anu, ndiye akwaniritsireni malipiro awo. Ena mwa inu alamule anzawo ndi zomwe zili mu chizolowezi monga kuwolowa

أَسْكِنُوهُنَّ مِنْ حَيْثُ سَكَنتُم مِّن وُجْدِكُمْ وَلَا تُضَآرُّوهُنَّ لِتُضَيِّقُوا۟
عَلَيْهِنَّ ۚ وَإِن كُنَّ أُو۟لَٰتِ حَمْلٍ فَأَنفِقُوا۟ عَلَيْهِنَّ حَتَّىٰ يَضَعْنَ حَمْلَهُنَّ ۚ
فَإِنْ أَرْضَعْنَ لَكُمْ فَـَٔاتُوهُنَّ أُجُورَهُنَّ ۖ وَأْتَمِرُوا۟ بَيْنَكُم بِمَعْرُوفٍ ۖ وَإِن
تَعَاسَرْتُمْ فَسَتُرْضِعُ لَهُۥٓ أُخْرَىٰ ﴿٦﴾ لِيُنفِقْ ذُو سَعَةٍ مِّن سَعَتِهِۦ ۖ
وَمَن قُدِرَ عَلَيْهِ رِزْقُهُۥ فَلْيُنفِقْ مِمَّآ ءَاتَىٰهُ ٱللَّهُ ۚ لَا يُكَلِّفُ ٱللَّهُ نَفْسًا
إِلَّا مَآ ءَاتَىٰهَا ۚ سَيَجْعَلُ ٱللَّهُ بَعْدَ عُسْرٍ يُسْرًا ﴿٧﴾ وَكَأَيِّن مِّن قَرْيَةٍ
عَتَتْ عَنْ أَمْرِ رَبِّهَا وَرُسُلِهِۦ فَحَاسَبْنَٰهَا حِسَابًا شَدِيدًا وَعَذَّبْنَٰهَا
عَذَابًا نُّكْرًا ﴿٨﴾ فَذَاقَتْ وَبَالَ أَمْرِهَا وَكَانَ عَٰقِبَةُ أَمْرِهَا خُسْرًا ﴿٩﴾
أَعَدَّ ٱللَّهُ لَهُمْ عَذَابًا شَدِيدًا ۖ فَٱتَّقُوا۟ ٱللَّهَ يَٰٓأُو۟لِى ٱلْأَلْبَٰبِ ٱلَّذِينَ ءَامَنُوا۟ ۚ
قَدْ أَنزَلَ ٱللَّهُ إِلَيْكُمْ ذِكْرًا ﴿١٠﴾ رَّسُولًا يَتْلُوا۟ عَلَيْكُمْ ءَايَٰتِ ٱللَّهِ مُبَيِّنَٰتٍ
لِّيُخْرِجَ ٱلَّذِينَ ءَامَنُوا۟ وَعَمِلُوا۟ ٱلصَّٰلِحَٰتِ مِنَ ٱلظُّلُمَٰتِ إِلَى ٱلنُّورِ ۚ
وَمَن يُؤْمِنۢ بِٱللَّهِ وَيَعْمَلْ صَٰلِحًا يُدْخِلْهُ جَنَّٰتٍ تَجْرِى مِن تَحْتِهَا
ٱلْأَنْهَٰرُ خَٰلِدِينَ فِيهَآ أَبَدًا ۖ قَدْ أَحْسَنَ ٱللَّهُ لَهُۥ رِزْقًا ﴿١١﴾ ٱللَّهُ ٱلَّذِى خَلَقَ
سَبْعَ سَمَٰوَٰتٍ وَمِنَ ٱلْأَرْضِ مِثْلَهُنَّ يَتَنَزَّلُ ٱلْأَمْرُ بَيْنَهُنَّ لِتَعْلَمُوٓا۟ أَنَّ
ٱللَّهَ عَلَىٰ كُلِّ شَىْءٍ قَدِيرٌ وَأَنَّ ٱللَّهَ قَدْ أَحَاطَ بِكُلِّ شَىْءٍ عِلْمًۢا ﴿١٢﴾

manja komanso kukoma mtima. Ngati simudzagwirizana zoti mayi wa mwanayo ayamwitse, ndiye kuti atatewo adzawayamwitsira woyamwitsa wina wosakhala mayi wosudzulidwayo.]

(7) Wopeza bwino apereke malinga ndi kupeza bwino kwake, ndipo amene wachepekedwera rizq lake, apereke (kangachepe) pa zomwe Allah wamupatsa. Allah sakakamiza kupatula zomwe wapereka (kwa munthu). Allah apereka kupeza bwino pambuyo pa masautso.

[Mwamuna apereke zomwe Allah wamupatsa kwa mkazi wake wosiidwa komanso kwa mwana wake ngati mwamunayo ali wopeza bwino pa rizq. Tsono amene wapatsidwa rizq lochepa ameneyo ndiye wosauka, apereke karizq mu zomwe wamupatsa Allah. Allah sakakamiza munthu wosauka mofanana ndi momwe amakakamizira munthu wolemera. Allah adzapereka kutambasuka mu rizq komanso kulemera pambuyo posauka ndi mavuto.]

(8) Eni midzi yambiri adanyoza lamulo la Mbuye wawo ndi aneneri Ake, ndipo ndidawawerengera ndi chiwerengero chokhwima (posanthula zochita zawo zonse). Ndiponso tidawalanga ndi chilango chaukali.

(9) Choncho adalawa kuipa kwa zinthu zawo ndipo mapeto a zinthu zawo adali kutayika (kuonongeka kwakukulu).

8-9 [Ndipo midzi yambiri eni ake adanyoza lamulo la Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndipo adapitiriza kukhala mu kupyola malire ndi ukafiri wawo, ndiye Ife tidawawerengera iwowo pa ntchito zawo pa dziko lapansi kuwawerengera kokhwima zedi ndipo tidawalanga ndi chilango chaukali , kotero adalawa mapeto woipa a kudzikuza ndi ukafiri wawo. Ndiye adali mapeto a ukafiri wawowo kuwonongeka ndi kutaika palibenso kutaika kwina pambuyo pake.]

(10) Allah wawakonzera iwo chilango chaukali, choncho, muopeni Allah, e, inu eni nzeru amene mwakhulupirira! Ndithudi Allah wavumbulutsa chikumbutso (cholemekezeka kwa inu).

(11) Mtumiki (SAW) akukuwerengerani ndime za Allah zolongosola (choonadi ndi chonama) kuti awatulutse mu mdima ndi kuwaika pa dangalira amene wakhulupirira ndi kumachita zabwino. Ndipo amene akhulupirira Allah ndi kumachita zabwino, adzamulowetsa m'minda momwe mitsinje ikuyenda pansi pake; akakhala m'menemo muyaya. Ndithu Allah wam'konzera iye rizq labwino.

10-11 [ Allah wawakonzera anthu amenewa omwe adapyola malire nasemphana ndi lamulo Lake ndi la atumiki Ake chilango chopweteka koopsa. Choncho inu eni nzeru amene mudamuvomera Allah ndi atumiki Ake nkugwiritsa ntchito malamulo Ake, opani Allah ndipo pewani mkwiyo Wake. Ndithudi Allah adavumbulutsa kwa inu e, inu okhulupirira chikumbutso chimene akukumbutsani nacho ndi kukumbutsaninso gawo lanu la chikhulupiriro mwa Allah ndi kugwira ntchito zomvera Iye. Chikumbutso chimenechi ndi Mtumiki (SAW) amene akukuwerengerani ndime za (Qur'aan) Allah zofotokozera kwa inu choonadi ku chabodza. (Watero) kuti awatulutse anthu amene adavomereza Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) namagwira ntchito molingana ndi zomwe Allah walamulira nkumamumvera, kuchoka ku mdima wa ukafiri kupita ku dangalira la chikhulupiriro. Ndipo amene akhulupirire mwa Allah nkumagwira ntchito zabwino , akamulowetsa ku minda yomwe pansi pa mitengo yake pakuyenda mitsinje. Akakhalamo muyaya. Ndithu Allah amukonzera bwinio rizq mu jannat munthu wokhulupirira wochita zabwino]

(12) Allah ndi Yemwe adalenga thambo zisanu ndi ziwiri nthakanso chimodzimodzi. Malamulo

Ake akutsika pakati pa izo kuti mudziwe kuti ndithu Allah pa chilichonse ndi wokhoza ndikutinso Allah wachizinga chilichonse m'kuchidziwa.

[Allah yekahyo ndi Amene adalenga thambo zisanu ndi ziwiri komanso nthaka chiwerengero chomwecho. Ndipo adatumiza lamulo mu zomwe wazivumbulutsa Iye kwa atumiki Ake ndi zomwe akuzikonzera zolengedwa Zake pakati pa mitambo ndi nthaka kuti inu anthu mudziwe kuti ndithu Allah ndi wokhoza kuchita chilichonse palibe chingamulephere Iye. Ndikutinso ndithu Allah wachizinga chinthu chilichonse kuchizindikira kotero palibe chimene chingatuluke mu kuzindikira ndi kuthekera Kwake.]

## (66) SURAT ATAHRIM

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) E, iwe Mneneri (SAW) n'chifukwa chiyani ukudziletsa chimene Allah wakuloleza kuchita? Ukufuna kukondweretsa akazi ako (n'chifukwa chake wachita izi?). Koma Allah Ngokhululuka kwambiri Ngwachisoni.

[E, iwe Mneneri, ndi chifukwa chiyani ukudziletsa zinthu zololedwa zimene Allah wakuloleza iweyo, kodi ukufuna kusangalatsa akazi ako? Ndipo Allah Ngokhululuka kwa iwe, Wachifundo nawe.]

(2) Ndithu, Allah wakhazikitsa (lamulo) lomasulira kulumbira kwanu, (inu anthu), ndipo Allah ndiye Mtetezi wanu. Iye Ngodziwa kwambiri ndiponso Ngwanzeru zakuya (pa malamulo amene wakhazikitsa kwa inu. [E, inu amene mwakhulupirira! Allah wakuikirani lamulo lomasulira kulumbira kwanu popereka dipo la zimenezo. Ili ndi kudyetsa anthu osauka khumi, kapena kuwaveka, kapena kumasula goli la kapolo. Ndipo amene sadapeze, ndiye kumanga (kusala) masiku atatu. Ndipo Allah akutetezani komanso ndi Muyang'aniri wa zinthu zanu zonse. Iye Ngodziwa za zomwe zikukhalireni bwino ndiye amazilamula kwa inu. Ngwanzeru zakuya mu zoyankhula ndi zochita Zake.]

(3) Kumbuka pamene Mneneri adauza wina mwa akazi ake nkhani (yachinsinsi), choncho (mkaziyo) pamene adaiulula, Allah adam'dziwitsa (Mtumiki SAW) za kuwululidwa kwa nkhaniyo, (ndipo Mtumiki SAW) adaifotokoza mbali ina ya nkhaniyo, koma mbali ina adaisiya. Pamene adafotokozera (mkazi wake) za nkhaniyo adati: "Ndani wakuuza zimenezi?" (Mtumiki SAW) adati: "Wandiuza Wodziwa kwambiri. Ndiponso Wodziwa zazing'ono ndi zazikulu (Amene sichibisika kwa Iye chobisika chilichonse).

[Kumbuka pa nthawi imene Mtumiki (SAW) adamuuza mwa mseri mkazi wake Hafswah

سُورَةُ التَّحْرِيمِ

ترتيبها ٦٦ — آياتها ١٢

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَٰنِ الرَّحِيمِ

يَا أَيُّهَا النَّبِيُّ لِمَ تُحَرِّمُ مَا أَحَلَّ اللَّهُ لَكَ تَبْتَغِي مَرْضَاتَ أَزْوَاجِكَ وَاللَّهُ
غَفُورٌ رَحِيمٌ ﴿١﴾ قَدْ فَرَضَ اللَّهُ لَكُمْ تَحِلَّةَ أَيْمَانِكُمْ وَاللَّهُ مَوْلَاكُمْ
وَهُوَ الْعَلِيمُ الْحَكِيمُ ﴿٢﴾ وَإِذْ أَسَرَّ النَّبِيُّ إِلَىٰ بَعْضِ أَزْوَاجِهِ حَدِيثًا
فَلَمَّا نَبَّأَتْ بِهِ وَأَظْهَرَهُ اللَّهُ عَلَيْهِ عَرَّفَ بَعْضَهُ وَأَعْرَضَ عَنْ بَعْضٍ
فَلَمَّا نَبَّأَهَا بِهِ قَالَتْ مَنْ أَنْبَأَكَ هَٰذَا قَالَ نَبَّأَنِيَ الْعَلِيمُ الْخَبِيرُ
﴿٣﴾ إِنْ تَتُوبَا إِلَى اللَّهِ فَقَدْ صَغَتْ قُلُوبُكُمَا وَإِنْ تَظَاهَرَا عَلَيْهِ
فَإِنَّ اللَّهَ هُوَ مَوْلَاهُ وَجِبْرِيلُ وَصَالِحُ الْمُؤْمِنِينَ وَالْمَلَائِكَةُ
بَعْدَ ذَٰلِكَ ظَهِيرٌ ﴿٤﴾ عَسَىٰ رَبُّهُ إِنْ طَلَّقَكُنَّ أَنْ يُبْدِلَهُ أَزْوَاجًا
خَيْرًا مِنْكُنَّ مُسْلِمَاتٍ مُؤْمِنَاتٍ قَانِتَاتٍ تَائِبَاتٍ عَابِدَاتٍ سَائِحَاتٍ
ثَيِّبَاتٍ وَأَبْكَارًا ﴿٥﴾ يَا أَيُّهَا الَّذِينَ آمَنُوا قُوا أَنْفُسَكُمْ وَأَهْلِيكُمْ
نَارًا وَقُودُهَا النَّاسُ وَالْحِجَارَةُ عَلَيْهَا مَلَائِكَةٌ غِلَاظٌ شِدَادٌ
لَا يَعْصُونَ اللَّهَ مَا أَمَرَهُمْ وَيَفْعَلُونَ مَا يُؤْمَرُونَ ﴿٦﴾ يَا أَيُّهَا
الَّذِينَ كَفَرُوا لَا تَعْتَذِرُوا الْيَوْمَ إِنَّمَا تُجْزَوْنَ مَا كُنْتُمْ تَعْمَلُونَ ﴿٧﴾

(RA) nkhani, ndipo pamene iye adauza nkhaniyo Aisha (RA) ndipo Allah atamuwonetsera zoululika kwa chinsinsi chija, Mtumiki (SAW) adamuuza Hafswah (RA) zimene iye adanena. Ndipo Mtumiki (SAW) adasiya mbali ina ya nkhaniyo wosaifotokoza pongolemekeza chabe. Pamene adamuuza zomwe iye (Hafswah RA) adafalitsa za nkhaniyo, iye adati : "Ndani wakuuza zimenezi?" Mtumiki (SAW) adati: "Wandiuza zimenezi ndi Allah Wodziwa, Wozindikira, Amene sikabisika pa Iye kobisika kalikonse.]

(4) (Amene adali ndi nsanje kwambiri mwa akazi ake ndi mayi Aishah (RA) ndi mayi Hafswah (RA). Ndipo Allah adawauza motere): Ngati awirinu mulapa kwa Allah pa zimene mwachita (chitani changu kulapa) chifukwa chakuti mitima yanu yapotoka pang'ono (chifukwa cha nsanje pa zimene Mneneri (SAW) akufuna zosunga chinsinsi chake), koma ngati awirinu muthandizana pa zimene zingamuvutitse, ndithu, Allah ndiye Mtetezi Wake komanso Jibril (Gabriel). Ndiponso Asilamu abwino, nawonso Angero; kuwonjezera apa ndi athandizi (ake). [Inu

awirinu (Hafswah ndi Aisha RA) ngati mutabwerera kwa Allah, ndithu zipezeka kwa inu zomwe zingakakamize kulapa poti mitima yanu idapendekera ku zomwe anadana nazo Mtumiki (SAW) zofalitsa chinsinsi chake. Ndipo ngati awirinu mutati muthandizane pa zomwe zingamuvutitse, ndiye kuti ndithu Allah ndi Mtetezi wake komanso Jibril (Gabriel) ndi abwino a okhulupirira ndinso Angero pambuyo pa chithandizo cha Allah, ndi athandizi ake polimbana ndi amene akumuvutitsa ndi kumuchita udani.]

(5) Ngati Mtumiki (SAW) akusudzulani, Mbuye wake am'patsa akazi ena m'malo mwa inu, abwino kuposa inu, ogonjera Allah, okhulupirira (ndi mitima yawo), omvera, olapa, odzichepetsa pa maso pa Allah (ochita mapemphero kwambiri), oyenda (pa chikhulupiriro cha Allah) kapena ochulukitsa kumanga; amene adakwatiwapo kale ndi osakwatiwapo.

[Mwina Mbuye wake ngati atakusiyani ukwati inu akazi a Mtumiki (SAW), angamukwatitse m'malo mwa inu akazi ogonjera Allah pa kumvera malamulo, okhulupirira mwa Allah ndi Mtumiki Wake (SAW), omvera Allah, obwerera ku zomwe amazikonda Allah zomvera Iye, ochulukitsa kuchita ibaadah, osala, ena mwa iwo oti adakwatiwapo ndinso osakwatiwapo.]

(6) E, inu amene mwakhulupirira! Dzitchinjirizeni inu ndi maanja anu ku moto umene nkhuni zake ndi anthu ndi miyala, oyang'anira ake ndi Angero ouma mitima, amphamvu. Sanyoza Allah pa zimene wawalamula, amachita (zokhazo) zimene alamulidwa.

[E, inu anthu amene mudamuvomereza Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndi kugwiritsa ntchito malamulo Ake! Dzisungeni nokha pochita zimene wakulamulani Allah ndi kusiya zimene wakuletsani. Ndipo sungani akubanja kwanu ndi zomwe mukudzisungira inu eni akenu ku moto umene nkhuni zake ndi anthu ndi miyala. Amene azikapereka chilango cha anthu akumeneko ndi angero amphamvu, ouma mitima pothana nawo iwowo, sanyoza Allah pa lamulo Lake ndipo amachita zimene alamulidwa kutero].

(7) (Adzawauza osakhulupirira pa Tsiku Lachiweruzo): E, inu amene simudakhulupirire! Musadandaule lero, ndithu mulipidwa pa zimene mumachita (pa dzikolapansi).

[Ndipo kudzanenedwa kwa anthu amene adakana zoti Allah ndiye Woyenerera kupembedzewa mwa choonadi namukana pa nthawi yowalowetsa ku moto kuti: "Musafunefune chowiringula pa tsiku la lero, ndithudi mukupatsidwa malipiro a zomwe mudali kuzichita pa dziko lapansi"]

(8) E, inu amene mwakhulupirira! Lapani kwa Allah, kulapa koona; ndithu Mbuye wanu akufafanizirani zoipa zanu ndi kukakulowetsani m'minda momwe mitsinje ikuyenda pansi pake, tsiku limene Allah sadzayalutsa Mtumiki (SAW) ndi amene adakhulupirira pamodzi naye. Dangalira lawo lidzayenda cha patsogolo pawo ndi mbali ya kumanja kwawo, uku akunena : "Mbuye wathu! Tikwaniritsireni dangalira lathu (mpaka likatifikitse ku munda wa mtendere), ndiponso khululukani machimo athu, ndithu Inu ndi Wokhoza chilichonse".[E, inu anthu amene mudamuvomereza Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndi kugwiritsa ntchito malamulo Ake! Bwererani kusiya machimo anu kupita komumvera Allah kubwerera kopandanso kubwereranso pambuyo pake, mwina Mbuye wanu angakufafanizireni zoipa za ntchito zanu, ndi kukalowetsani m'minda yomwe ikuyenda pansi pa nyumba zake za chifumu mitsinje. Tsiku lomwe Allah sadzayalutsa Mtumiki (SAW) ndi anthu amene adakhulupirira limodzi naye ndipo sadzawalanga koma adzakweza zinthu zawo (kakhalidwe kawo). Dangalira la amenewa lizidzayenda patsogolo pawo ndi ku dzanjadzanja kwawo uku akunena kuti: "Mbuye wathu tikwaniritsireni dangalira lathu kufikira titawoloka pa mulatho (swirat) ndi kuti tiwongoleredwe kukalowa ku Jannat, ndipo tifafanizireni ife ndi kutikhululukira machimo athu ndi kutibisira ifeyo, ndithudi inu muli ndi kuthekera pa kanthu kena kalikonse.]

(9) E, iwe Mneneri (SAW)! Limbana ndi akafiri (osakhulupirira) ndi amunafikina (achiphamaso), aumire mtima. Malo awo ndi ku Jahannama (taonani) kuipa kobwerera (kwawo)!

[E, iwe Mneneri (SAW) ! Limbana nawo anthu amene awonetsera ukafiri ndi kuwulengeza. Ndipo chita nawo nkhondo ndi lupannga komanso ulimbane nawo anthu amene akubisa ukafiri kudzera mukuwiringula ndi kuimika malamulo ndi zisonyezo za chipembedzo. Ndipo ugwiritsire mphamvu ndi kuwuma mtima pa magulu awiri onsewo polimbana nawo. Ndipo malo awo amene adzathere iwowo pa Tsiku Lomaliza ndi ku Jahannama, kotero nkoipa kobwerera kwawo kumene adzabwerere kumeneko.]

(10) Allah wapereka fanizo la osakhulupirira monga mkazi wa Noah (AS) ndi mkazi wa Luti (AS). Awiriwa adali pansi pa akapolo

يَٰٓأَيُّهَا ٱلَّذِينَ ءَامَنُواْ تُوبُوٓاْ إِلَى ٱللَّهِ تَوۡبَةٗ نَّصُوحًا عَسَىٰ رَبُّكُمۡ
أَن يُكَفِّرَ عَنكُمۡ سَيِّـَٔاتِكُمۡ وَيُدۡخِلَكُمۡ جَنَّٰتٖ تَجۡرِي
مِن تَحۡتِهَا ٱلۡأَنۡهَٰرُ يَوۡمَ لَا يُخۡزِي ٱللَّهُ ٱلنَّبِيَّ وَٱلَّذِينَ ءَامَنُواْ
مَعَهُۥۖ نُورُهُمۡ يَسۡعَىٰ بَيۡنَ أَيۡدِيهِمۡ وَبِأَيۡمَٰنِهِمۡ يَقُولُونَ رَبَّنَآ
أَتۡمِمۡ لَنَا نُورَنَا وَٱغۡفِرۡ لَنَآۖ إِنَّكَ عَلَىٰ كُلِّ شَيۡءٖ قَدِيرٞ ٨
يَٰٓأَيُّهَا ٱلنَّبِيُّ جَٰهِدِ ٱلۡكُفَّارَ وَٱلۡمُنَٰفِقِينَ وَٱغۡلُظۡ عَلَيۡهِمۡۚ
وَمَأۡوَىٰهُمۡ جَهَنَّمُۖ وَبِئۡسَ ٱلۡمَصِيرُ ٩ ضَرَبَ ٱللَّهُ مَثَلٗا
لِّلَّذِينَ كَفَرُواْ ٱمۡرَأَتَ نُوحٖ وَٱمۡرَأَتَ لُوطٖۖ كَانَتَا تَحۡتَ
عَبۡدَيۡنِ مِنۡ عِبَادِنَا صَٰلِحَيۡنِ فَخَانَتَاهُمَا فَلَمۡ يُغۡنِيَا عَنۡهُمَا
مِنَ ٱللَّهِ شَيۡـٔٗا وَقِيلَ ٱدۡخُلَا ٱلنَّارَ مَعَ ٱلدَّٰخِلِينَ ١٠
وَضَرَبَ ٱللَّهُ مَثَلٗا لِّلَّذِينَ ءَامَنُواْ ٱمۡرَأَتَ فِرۡعَوۡنَ إِذۡ
قَالَتۡ رَبِّ ٱبۡنِ لِي عِندَكَ بَيۡتٗا فِي ٱلۡجَنَّةِ وَنَجِّنِي مِن فِرۡعَوۡنَ
وَعَمَلِهِۦ وَنَجِّنِي مِنَ ٱلۡقَوۡمِ ٱلظَّٰلِمِينَ ١١ وَمَرۡيَمَ ٱبۡنَتَ
عِمۡرَٰنَ ٱلَّتِيٓ أَحۡصَنَتۡ فَرۡجَهَا فَنَفَخۡنَا فِيهِ مِن رُّوحِنَا
وَصَدَّقَتۡ بِكَلِمَٰتِ رَبِّهَا وَكُتُبِهِۦ وَكَانَتۡ مِنَ ٱلۡقَٰنِتِينَ ١٢

Athu awiri abwino, koma adali osakhulupirika kwa amuna awo, (ndipo amuna awo) sadawateteze kalikonse ku chilango cha Allah,ndipo kudanenedwa kwa iwo: "Lowani ku moto pamodzi (ndi ena) olowa."[Allah waika fanizo la kakhalidwe ka anthu amene adakanira Allah pa kasankhaniridwe kawo ndi Asilamu ndi kuyandikira kwawo kwa iwo ndi kukhalirana kwawo limodzi –ndikuti zimenezo sizingathandize iwowo chifukwa chokanira kwawo kwa Allah- ndi kakhalidwe ka mkazi wa mneneri wa Allah Noah (AS) ndi mkazi wa Mneneri Luti (AS): Pamene awiriwa adali m'manja mwa akapolo awiri mwa akapolo Athu olungama. Ndipo kudachitika kwa awiriwa chinyengo chowachita aneneriwa mu chipembedzo. Awiriwa adali okanira Allah ndipo Atumiki awiriwa sadatchinjirize kalikonse akazi awo awiriwa ku chilango cha Allah. Ndipo kudanenedwa kwa akazi awiriwa kuti: "Lowani ku moto limodzi ndi olowa m'menemo." Poika chitsanzo chimenechi muli umboni wosonyeza kuti ndithudi kuyandikira kwa Aneneri ndi olungama, sikuthandiza kalikonse limodzi ndi ntchito zoipa.]

(11) Ndiponso Allah wapereka fanizo la amene akhulupirira monga mkazi wa Firauna (Farawo) pamene adanena : "Mbuye wanga! Ndimangireni, kwa Inu, nyumba mu Jannat, ndipo ndipulumutseni kwa Farawo ndi zochita zake, ndiponso ndipulumutseni kwa anthu oipa ndi amtopola."[Ndipo Allah waika fanizo la kakhalidwe ka anthu okhulupirira- amene adamuvomereza Allah, namupembedza Iye Yekha, nagwiritsa ntchito malamulo Ake ndikuti iwowo sikungavutitse kusakanikirana ndi makafiri mu kukhalirana nawo iwo – ndi m'mene adalili mkazi wa Farawo amene adali pansi pa munthu wokanira Allah molapitsa kuposa onse okanira Iye, iye (mkaziyo) ali wokhulupirira, pamene iye adati: "Mbuye wanga! Ndimangireni ine nyumba kwa Inu mu jannat, ndipo ndipulumutseni ku mphamvu za Farawo ndi mayesero ake ndi zomwe zikuchokera kwa iye mu ntchito zoipa, komanso ndipulumutseni kwa amene akutsata iye mu kupondereza ndi kusokera komanso ku chilango chawo.]

(12) Ndi (fanizo lina la okhulupirira monga) Mariyamu mwana wa Imran amene adasunga umaliseche wake; ndipo tidauzira m'menemo mzimu Wathu ndipo adavomereza mawu a Mbuye wake (omwe adali zolamula ndi zoletsa Zake) ndi mabuku Ake (amene adavumbulutsidwa kwa aneneri Ake); adali m'modzi wa opitiriza kudzichepetsa ndi kumvera Allah. [Ndipo Allah wapereka fanizo la anthu amene adakhulupirira, Mariamu mwana wa Imurani amene adasunga maliseche ake, nawasamala ku chiwerewere, ndipo Allah adalamula Jibril (AS) kuti auzire mpweya povalira malaya ake ndipo udakafika ku chiberekero chake natenga mimba ya Issa (AS) ndipo adavomereza mawu a Mbuye wake. Komanso adagwiritsa ntchito malamulo Ake amene adawalamulira akapolo Ake ndi mabuku Ake amene adawavumbulutsa kwa Atumiki Ake (AS) ndipo iye adali m'gulu la anthu omvera Iye.]

## (67) SURAT-UL- MULK

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Watukuka ndi kudalitsika Amene m'manja Mwake muli ufumu (wochita chilichonse pa zolengedwa zonse); ndipo Iye ali ndi mphamvu yokwanira pa chilichonse.

[Zachuluka zabwino za Allah ndi ubwino Wake pa zolengedwa Zake zonse. Amene m'manja Mwake muli ufumu wa dziko lapansi ndi Tsiku Lomaliza ndi mphamvu za zinthu ziwirizi. Lamulo ndi chigamulo Chake chimachitika mu ziwirizi, ndipo Iye pa chinthu

ترتيبها ٦٧ — سُورَةُ المُلْكِ — آياتها ٣٠

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَٰنِ الرَّحِيمِ

تَبَارَكَ الَّذِي بِيَدِهِ الْمُلْكُ وَهُوَ عَلَىٰ كُلِّ شَيْءٍ قَدِيرٌ ﴿١﴾ الَّذِي خَلَقَ
الْمَوْتَ وَالْحَيَاةَ لِيَبْلُوَكُمْ أَيُّكُمْ أَحْسَنُ عَمَلًا ۚ وَهُوَ الْعَزِيزُ الْغَفُورُ ﴿٢﴾
الَّذِي خَلَقَ سَبْعَ سَمَاوَاتٍ طِبَاقًا ۖ مَّا تَرَىٰ فِي خَلْقِ الرَّحْمَٰنِ مِن
تَفَاوُتٍ ۖ فَارْجِعِ الْبَصَرَ هَلْ تَرَىٰ مِن فُطُورٍ ﴿٣﴾ ثُمَّ ارْجِعِ الْبَصَرَ كَرَّتَيْنِ
يَنقَلِبْ إِلَيْكَ الْبَصَرُ خَاسِئًا وَهُوَ حَسِيرٌ ﴿٤﴾ وَلَقَدْ زَيَّنَّا السَّمَاءَ
الدُّنْيَا بِمَصَابِيحَ وَجَعَلْنَاهَا رُجُومًا لِّلشَّيَاطِينِ ۖ وَأَعْتَدْنَا لَهُمْ عَذَابَ
السَّعِيرِ ﴿٥﴾ وَلِلَّذِينَ كَفَرُوا بِرَبِّهِمْ عَذَابُ جَهَنَّمَ ۖ وَبِئْسَ الْمَصِيرُ
﴿٦﴾ إِذَا أُلْقُوا فِيهَا سَمِعُوا لَهَا شَهِيقًا وَهِيَ تَفُورُ ﴿٧﴾ تَكَادُ تَمَيَّزُ
مِنَ الْغَيْظِ ۖ كُلَّمَا أُلْقِيَ فِيهَا فَوْجٌ سَأَلَهُمْ خَزَنَتُهَا أَلَمْ يَأْتِكُمْ نَذِيرٌ ﴿٨﴾
قَالُوا بَلَىٰ قَدْ جَاءَنَا نَذِيرٌ فَكَذَّبْنَا وَقُلْنَا مَا نَزَّلَ اللَّهُ مِن شَيْءٍ إِنْ أَنتُمْ
إِلَّا فِي ضَلَالٍ كَبِيرٍ ﴿٩﴾ وَقَالُوا لَوْ كُنَّا نَسْمَعُ أَوْ نَعْقِلُ مَا كُنَّا فِي أَصْحَابِ
السَّعِيرِ ﴿١٠﴾ فَاعْتَرَفُوا بِذَنبِهِمْ فَسُحْقًا لِّأَصْحَابِ السَّعِيرِ ﴿١١﴾
إِنَّ الَّذِينَ يَخْشَوْنَ رَبَّهُم بِالْغَيْبِ لَهُم مَّغْفِرَةٌ وَأَجْرٌ كَبِيرٌ ﴿١٢﴾

chilichonse ali nako kuthekera. Ndipo zikuphunzitsidwa kuchokera mu ndime imeneyi kukhazikika kwa mbiri yokhala ndi dzanja kwa Allah Subhaanahu Wataalaa pa zomwe zili zoyenerera ulemerero Wake.]

(2) Amene walenga imfa ndi moyo kuti akuyeseni (mayeso) ndani mwa inu ali wochita zabwino (kwambiri). Ndipo Iye ndi Wopambana mu mphamvu (salephera kanthu) ndiponso wokhululukira olakwa. [Amene adalenga imfa ndi moyo kuti akuyeseni – inu anthu- kuti ndi ndani mwa inu achite bwino kwambiri ntchito ndi kudziyeretsa? Iye ndi Wamphamvu Amene palibe chinthu chilichonse chimene chingamulephere, Wokhululukira amene walapa mwa akapolo Ake. Mu ndime imeneyi muli chirimbikitso mu kuchita zinthu zomumvera Iye ndi chiletso cha kuchita machimo.]

(3) Amene adalenga thambo zisanu ndi ziwiri mosanjikana (kapena zolingana m'kalengedwe kake). Siuwona kusiyana m'zolengedwa za Wachifundo chambiri. Bwereza kuyang'ana; kodi ukuona pena pong'ambika? [Amene adalenga thambo zisanu ndi ziwiri zosanjikana zina pamwamba pa zimnzake. Siungaone mu kulenga kwa Allah – e, iwe woyang'ana- kusemphana kuli konse kapena kusiyana. Ndipo bwerezanso kuyang'ana kumwamba, kodi ukuwona m'menemo ming'alu ili yonse kapena kung'ambika?]

4 (4) Bwerezanso kuyang'ana kachiwiri, kuyang'anako kukubwerera wekha (uku maso) ali olobodoka ndiponso otopa (siuwona polakwika paliponse).
[Kenako bwerezanso kuyang'ana kamodzi pambuyo pa kena, abwerera kwa iwe maso ali olobodoka, ochepera mphamvu kuti aone kupunguka kuli konse ali otopa opanda mphamvu.]

(5) Ndithu, talikongoletsa thambo loyandikirali ndi nyali (nyenyezi) ndipo tazichita kukhala (mochokera zenje) zolasila asatana. Ndipo tawakonzera (pa Tsiku Lomaliza) chilango chamoto woyaka.
[Ndithudi takongoletsa thambo loyandikira limene maso akuliwonali ndi nyenyezi zowala zikuluzikulu. Ndipo tazichita kukhala zenje zotenthera amene akukaba kumvetsera za kumwamba m'gulu la asatana. Komanso tidawakonzera iwowo mu Tsiku Lomaliza chilango cha moto woyaka umene akaumve kutentha kwake.]

(6) Ndipo kwa amene sakhulupirira Mbuye wawo ali nacho chilango cha Jahannama, ndipo kuipirenji kobwerera!
[Ndipo ali nacho anthu okanira Mbuye wawo chilango cha jahannama ndipo ngoipitsitsa malo wobwerera awo ku jahannama.]

(7) Akadzaponyedwa m'menemo, adzamva mkokomo wake (oipa) uku ukuwira mwaukali.
[Makafiri amenewa akakaponyedwa mu jahannama akaimva mawu woipitsitsa kwambiri, umenewo ukuwira kwam'nanu.]

(8) Udzayandikira kuphwasuka chifukwa cha mkwiyo (kukwiira oipa); nthawi iliyonse gulu (la oipa) likadzaponyedwa m'menemo, angero oyang'anira motowo adzawafunsa (mowadzudzula); "kodi sadakufikireni mchenjezi (wokuchenjezani za tsikuli)?"
[Idzayandikira jahannama kung'ambika chifukwa cha kupsa mtima kwake kolapitsa kupsera anthu okanira Allah, nthawi ili yonse imene azikaponyedwamo gulu la anthu, azikawafunsa amene aikidwa kuyang'anira Jahannamayo mu njira yonyazitsa kuti: "Kodi sadakudzereni pa dziko lapansi mtumiki wokuchenjezani chilango chimenechi chimene inuyo mulichi?"]

(9) Adazyankha: "Inde adatifikira mchenjezi koma tidatsutsa, ndipo tidati Allah sadavumbulutse chilichonse (kwa iwe ngakhale kwa amnzako);

وَأَسِرُّواْ قَوۡلَكُمۡ أَوِ ٱجۡهَرُواْ بِهِۦٓۖ إِنَّهُۥ عَلِيمُۢ بِذَاتِ ٱلصُّدُورِ ١٣ أَلَا
يَعۡلَمُ مَنۡ خَلَقَ وَهُوَ ٱللَّطِيفُ ٱلۡخَبِيرُ ١٤ هُوَ ٱلَّذِي جَعَلَ لَكُمُ
ٱلۡأَرۡضَ ذَلُولٗا فَٱمۡشُواْ فِي مَنَاكِبِهَا وَكُلُواْ مِن رِّزۡقِهِۦۖ وَإِلَيۡهِ ٱلنُّشُورُ
١٥ ءَأَمِنتُم مَّن فِي ٱلسَّمَآءِ أَن يَخۡسِفَ بِكُمُ ٱلۡأَرۡضَ فَإِذَا هِيَ
تَمُورُ ١٦ أَمۡ أَمِنتُم مَّن فِي ٱلسَّمَآءِ أَن يُرۡسِلَ عَلَيۡكُمۡ حَاصِبٗاۖ
فَسَتَعۡلَمُونَ كَيۡفَ نَذِيرِ ١٧ وَلَقَدۡ كَذَّبَ ٱلَّذِينَ مِن قَبۡلِهِمۡ فَكَيۡفَ
كَانَ نَكِيرِ ١٨ أَوَلَمۡ يَرَوۡاْ إِلَى ٱلطَّيۡرِ فَوۡقَهُمۡ صَٰٓفَّٰتٖ وَيَقۡبِضۡنَۚ مَا
يُمۡسِكُهُنَّ إِلَّا ٱلرَّحۡمَٰنُۚ إِنَّهُۥ بِكُلِّ شَيۡءِۢ بَصِيرٌ ١٩ أَمَّنۡ هَٰذَا ٱلَّذِي
هُوَ جُندٞ لَّكُمۡ يَنصُرُكُم مِّن دُونِ ٱلرَّحۡمَٰنِۚ إِنِ ٱلۡكَٰفِرُونَ إِلَّا فِي غُرُورٍ
٢٠ أَمَّنۡ هَٰذَا ٱلَّذِي يَرۡزُقُكُمۡ إِنۡ أَمۡسَكَ رِزۡقَهُۥۚ بَل لَّجُّواْ فِي عُتُوّٖ
وَنُفُورٍ ٢١ أَفَمَن يَمۡشِي مُكِبًّا عَلَىٰ وَجۡهِهِۦٓ أَهۡدَىٰٓ أَمَّن يَمۡشِي سَوِيًّا
عَلَىٰ صِرَٰطٖ مُّسۡتَقِيمٖ ٢٢ قُلۡ هُوَ ٱلَّذِيٓ أَنشَأَكُمۡ وَجَعَلَ لَكُمُ ٱلسَّمۡعَ
وَٱلۡأَبۡصَٰرَ وَٱلۡأَفۡـِٔدَةَۖ قَلِيلٗا مَّا تَشۡكُرُونَ ٢٣ قُلۡ هُوَ ٱلَّذِي ذَرَأَكُمۡ
فِي ٱلۡأَرۡضِ وَإِلَيۡهِ تُحۡشَرُونَ ٢٤ وَيَقُولُونَ مَتَىٰ هَٰذَا ٱلۡوَعۡدُ إِن كُنتُمۡ
صَٰدِقِينَ ٢٥ قُلۡ إِنَّمَا ٱلۡعِلۡمُ عِندَ ٱللَّهِ وَإِنَّمَآ أَنَا۠ نَذِيرٞ مُّبِينٞ ٢٦

koma inu muli m'kusokera kwakukulu".

[Adzayankha kunena kuti: "Indedi adatifikira mtumiki wochokera kwa Allah ndipo adatichenjeza ife nkumukanira ndipo tidanena mu zinthu zimene adabweretsa mu maayat kuti "palibe kalikonse kamene Allah wavumbulutsa kwa aliyense mwa anthu, ndipo inu – atumikinu- simuli kalikonse koma kupita kutali kwambiri posiya choonadi].

10 Ndipo adzanena: "Tidakakhala kuti tidamvera (zimene ankatiuza) kapena kuziganizira mwa nzeru, sitidakakhala m'gulu la anthu a ku moto.

[Adzanena movomereza kuti : "Tikadakhala kuti tikumva momwe amverera munthu wofuna chowona, kapena kuganiza mu zomwe ife tikuitanidwira ku zimenezo, sibwenzi tili mu chiwerengero cha anthu a ku moto.]

11 Choncho adzavomereza machimo awo (koma sipadzakhala chopindula;) kuonongeka ndikukhala kutali (ndi chifundo cha Allah) kuli kwa anthu a ku moto!

[Ndipo adzavomereza kukanira kwawo ndi ukafiri wawo umene ayenerera nawo kupeza chilango cha moto, choncho ngotalikitsidwa ku chifundo cha Allah anthu a ku moto].

12 Ndithudi amene akumuopa Mbuye wawo pomwe iwo sakumuona, adzapeza chikhululuko pa machimo awo ndi malipiro aakulu (pa zabwino zomwe ankachita).

[Ndithu anthu amene akuopa Mbuye wawo, namamupembedza , namapanda kumunyoza iwo kulibe ku maso a anthu, namawopa chilango mu Tsiku Lomaliza asadachiwone, iwowo ali nako kufafaniziridwa machimo awo kwa Allah komanso malipiro aakulu amene ali jannat.]

13 Bisani mawu anu kapena awonetsereni poyera; (zonsezi n'chimodzimodzi kwa Allah) ndithudi Iye Ngodziwa zobisika za m'mitima.

[Bisani mawu anu – inu anthu- mu chinthu chilichonse mu zinthu zanu kapena awonetsereni poyera, ziwirizi kwa Allah n'zofanana. Ndithudi Iyeyo Subhaanahu Ngodziwa zobisa za mitima choncho mwa mtundu wanji zibisike kwa Iye zoyankhula ndi zochita zanu?]

14 Kodi asadziwe Amene adalenga (zinthu zonse)? Pomwe Iye Ngodziwa zinthu zing'onozing'ono kwambiri m'mene zilili (ndiponso) Ngodziwa nkhani zonse.

[Kodi asadziwe Mbuye wa zolengedwa zonse zolengedwa Zake ndi m'mene zilili kumachita kuti Iye ndi Amene adazilenga nkuzikonza bwino? Iye Ngodekha ndi akapolo Ake, Wozindikira za ntchito zawo zonse.]

15 Iye ndi Amene wakupangirani nthaka kuti ikhale yogonjera ( pa chilichonse chimene mufuna). Choncho yendani mbali zake zonse ndipo idyani riziq la m'menemo, (limene Allah akukutulutsirani). Kwa Iye yekha ndiko kobwerera kwanu (nonse mutapatsidwa moyo wachiwiri). [Allah Yekhayo ndi amene adakuchitirani nthaka kukhala yofewa, yolinganizidwa imene inu mumakhazikika pamenepo. Choncho yendani mbali zake zonse ndipo idyani riziq la Allah limene akukutulutsirani kuchokera m'menemo ndipo kwa Iye Yekhayo ndiko kumene mudzaukitsidwe kuchokera mmamda anu kuti mukawerengeredwe ntchito zanu ndi kulipidwa. Mu ndime imeneyi muli kulozera kofunafuna riziq ndi kugwira ntchito. Ndiponso mu ndime yomweyi muli umboni woti Allah Yekhayo, ndiye Wopembedzedwa Wachoonadi, palibe wothandizana Naye, chisonyezo cha kuthekera Kwake, chikumbutso cha mtendere Wake ndi chenjezo la kuyedzamira za m'dziko lapansi lokha.]

16 Kodi muli ndi chitetezo kwa Amene ufumu Wake uli kumwamba kuti sangakukwirireni mu nthaka (ndi kukudzidzimutsani) pamene nthaka ikugwedezeka molimba?

(17) Kapena kodi mwadziteteza kwa Amene ufumu Wake uli kumwamba kuti sangakutsitsireni mphepo yamkuntho ya miyala (ndi kukuonongani ndi miyalayo?) choncho mudzadziwa m'mene lili chenjezo Langa (pa inu).

16-17 [Kodi inu makafiri a pa Makka muli pa chitetezo cha Allah Amene ali pamwamba pa thambo kuti sangakukwirireni mu nthaka, mwadzidzidzi nkuiona ikukugwedezani kufikira mutaonongeka? Kapena mwadziika pa chitetezo cha Allah Amene ali pamwamba pa thambo kuti sangakutumizireni mphepo yamkuntho ikukugendani ndi miyala ing'onoing'ono? Ndipo mudzadziwa inu makafiri momwe chenjezo Langa lilili kwa inu pa nthawi imene mudzachione chilango ndipo sikudzakuthandizani kuzindikira nthawi imeneyo. Mu ndime imeneyi muli chitsimikizo chakuti upamwambamwamba ndi wa Allah Taalaa momwe ukuyenerera ndi ulemerero Wake Subhaanahu].

(18) Ndithudi amene adalipo kale iwo asanabadwe adakana atumuki awo. Nanga udali bwanji mkwiyo Wanga pa iwo ( pa kuwaononga onse)!

[Ndithudi adakanira atumiki awo anthu amene adalipo kale asadadze makafiri a pa Makka monga anthu a Noah, Aadu ndi Thamuud. Ndiye kudali bwanji kuipidwa Kwanga pa iwo ndi kuwatembenuzira mtendere umene anali nawo powatsitsira chilango ndi kuwaononga?]

(19) Kodi sadaione mbalame pamwamba pawo m'mene ikutambasulira (mapiko ake) ndi kuwafumbata. Palibe amene akuigwira kuti isagwe koma (Allah) Wachifundo chambiri; ndithudi Iye pa chilichonse Ngopenya.

(20) Kodi ndani amene ali asilikali anu okutetezani ku chilango posakhala (Allah) Wachifundo chambiri? Ndithudi osakhulupirira ali m'chinyengo.

(21) Kodi ndani angakupatseni riziq (limene mungakhalire ndi moyo ndi kupezera mtendere) ngati Iye atatsekereza riziq Lake (kwa inu)? Koma akafiri akupitiriza kudzikweza kwawo, kudziika kutali ndi choonadi.

19,20,21 > [Kodi sadazindikire makafiri amenewa ndipo sadaone mbalame pamwamba pawo zitatambasula mapiko ake pa nthawi youluka ndi kuwafumbata nthawi zina? Palibe amene amazisunga kuti zisagwe kupatula Wachifundo (Allah). Ndithudi Iye pa chinthu chili chonse Ngoyang'ana. Simuoneka mu zolengedwa Zake kupunguka kuli konse kapena kusiyana. Koma kodi ndi ndani uyo amene mukudzinamiza kwanu - inu makafiri - amene angakutetezeni popanda Wachifundo akakufunirani choipa? Makafiriwa mukudzinamiza kwawo sali kalikonse koma mu kunyengeka ndi kusokera kochokera kwa satana. Koma kodi ndi ndani uyo amene ali wopereka riziqi wabodzayu amene angamakupatseni riziq ngati Allah atakumanani riziq Lake? Koma kuti makafiri apitiriza mu kupyola kwawo malire ndi kusokera kwawo mwa mankhalu ndi kudzikweza ndinso kutalikira ku choonadi. Samamumvera Iye komanso samamutsatira.]

(22) Kodi amene akuyenda mozolika nkhope yake angakhale wowongoka kapena amene akuyenda molungama pa njira yosakhota?

[Kodi amene akuyenda atazolika nkhope yake asakudziwa kumene akuyenda ndi m'mene akupitira angakhale wowongoka kwambiri pa njira kapena amene akuyenda molungama chiriri ali bwinobwino pa njira yowongoka yosakhotakhota? Ili ndi fanizo limene Allah walipereka kwa kafiri ndi wokhulupirira.]

(23) Nena: "Iye ndi Amene adakulengani (pomwe simudali kanthu) ndipo adakupatsani makutu, maso ndi mitima (zimene mukhoza kupeza nazo mtendere); koma kuyamika kwanu (kwa Yemwe adakupatsani zimenezi) nkochepa kwambiri.

(24) Nena: "Iye ndi Amene adakulengani pa dziko ndipo kwa Iye (Yekha) ndiko mudzasonkhanitsidwa (kuti adzakuwerengereni ndi kukulipirani)

23-24 > [Nena kwa iwo iwe Mtumiki SAW kuti: "Allah ndi Amene adachititsa kuti inu mupezeke kuchokera kosakhala kalikonse, ndipo adakuchitirani makutu kuti mudzimverera nawo ndi maso kuti mudziyang'anira nawo ndi mitima kuti mudzikhala nayo ndi nzeru. Ndi zochepa zedi- inu makafiri- zimene mukupereka pothokoza mtendere wa Mbuye wanu umene adaupereka pa inu. Nena kwa iwo: "Allah ndi Amene adakulengani ndikukufalitsani pa nthaka, ndipo kwa Iye Yekhayo mudzasonkhanitsidwa pambuyo pakusiyana kumeneku kuti mukawerengeredwe ntchito zanu ndi kulipidwa".]

(25) Ndipo akunena (osakhulupirira za kuuka monyada): "Ndiliti lidzakwaniritsidwe) lonjezo ili ngati inu muli oona?

(26) Nena (iwe Mtumiki SAW): "Ndithu kudziwa (kwa izi) nkwa Allah Yekha; ndithudi ine , ndine mchenjezi wowonekera."

25-26 > [Ndipo akunena makafiri: "Kodi ndiliti lidzachitike lonjezo losonkhanitsidwali iwe Muhammad (SAW)? Tiuzeni za nthawi yake inu okhulupirira ngati mukunenadi zoona pa zimene mukunenazi." Nena iwe Mtumiki

فَلَمَّا رَأَوۡهُ زُلۡفَةٗ سِيٓـَٔتۡ وُجُوهُ ٱلَّذِينَ كَفَرُواْ وَقِيلَ هَٰذَا ٱلَّذِي
كُنتُم بِهِۦ تَدَّعُونَ ٢٧ قُلۡ أَرَءَيۡتُمۡ إِنۡ أَهۡلَكَنِيَ ٱللَّهُ وَمَن مَّعِيَ
أَوۡ رَحِمَنَا فَمَن يُجِيرُ ٱلۡكَٰفِرِينَ مِنۡ عَذَابٍ أَلِيمٖ ٢٨ قُلۡ هُوَ
ٱلرَّحۡمَٰنُ ءَامَنَّا بِهِۦ وَعَلَيۡهِ تَوَكَّلۡنَاۖ فَسَتَعۡلَمُونَ مَنۡ هُوَ فِي ضَلَٰلٖ مُّبِينٖ
٢٩ قُلۡ أَرَءَيۡتُمۡ إِنۡ أَصۡبَحَ مَآؤُكُمۡ غَوۡرٗا فَمَن يَأۡتِيكُم بِمَآءٖ مَّعِينِۭ ٣٠

ترتيبها ٦٨ — سُورَةُ القَلَمِ — آياتها ٥٢

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

نٓۚ وَٱلۡقَلَمِ وَمَا يَسۡطُرُونَ ١ مَآ أَنتَ بِنِعۡمَةِ رَبِّكَ بِمَجۡنُونٖ ٢
وَإِنَّ لَكَ لَأَجۡرًا غَيۡرَ مَمۡنُونٖ ٣ وَإِنَّكَ لَعَلَىٰ خُلُقٍ عَظِيمٖ ٤
فَسَتُبۡصِرُ وَيُبۡصِرُونَ ٥ بِأَييِّكُمُ ٱلۡمَفۡتُونُ ٦ إِنَّ رَبَّكَ هُوَ
أَعۡلَمُ بِمَن ضَلَّ عَن سَبِيلِهِۦ وَهُوَ أَعۡلَمُ بِٱلۡمُهۡتَدِينَ ٧ فَلَا تُطِعِ
ٱلۡمُكَذِّبِينَ ٨ وَدُّواْ لَوۡ تُدۡهِنُ فَيُدۡهِنُونَ ٩ وَلَا تُطِعۡ كُلَّ
حَلَّافٖ مَّهِينٍ ١٠ هَمَّازٖ مَّشَّآءِۭ بِنَمِيمٖ ١١ مَّنَّاعٖ لِّلۡخَيۡرِ مُعۡتَدٍ
أَثِيمٍ ١٢ عُتُلِّۭ بَعۡدَ ذَٰلِكَ زَنِيمٍ ١٣ أَن كَانَ ذَا مَالٖ وَبَنِينَ
١٤ إِذَا تُتۡلَىٰ عَلَيۡهِ ءَايَٰتُنَا قَالَ أَسَٰطِيرُ ٱلۡأَوَّلِينَ ١٥

(SAW) kwa amenewa kuti: "Ndithudi kuzindikira kwa nthawi yobwera Kiyama wadzisankhira yekha Allah, ndipo ine sindine kalikonse koma mchenjezi kwa inu kudzakuopsezani mapeto oipa a ukafiri wanu ndi kudzakulongosolerani zimene Allah wandilamula kuzifotokoza mwamvemvemve.]

27 Koma akadzaziona (zimene akulonjezedwazo) zili pafupi (ndi iwo), nkhope za amene sadakhulupirire zidzakhumudwa ndi kuyaluka kwambiri ndipo zidzanenedwa (mowadzudzula): "Izi ndi zija mudali kuzipempha (kuti zidze, zadza tsopano).

[Pamene makafiri adzaone chilango cha Allah chitayandikira kwa iwo ndi kuchiona diso kwa diso, kudzaonekera kuyaluka ndi kukhumudwa pa nkhope zawo. Ndipo kudzanenedwa mowanyanzitsa kuti: "Izi ndi zimene mudali kuzifuna kuti zibwere msanga pa dziko lapansi."

28 Nena (iwe Mtumiki SAW): "Tandiuzani ngati Allah atandiononga pamodzi ndi amene ndili nawo (monga momwe mukufunira) kuti kutichitira chifundo (ndi kutalikitsa nthawi ya moyo wathu). Nanga ndani amene adzawateteze osakhulupirira ku chilango chowawa?"

[Nena iwe Mtumiki (SAW) kwa anthu makafiri amenewa: "Tandiuzani ngati Allah atapereka imfa kwa ine ndi amene ndili nawo mwa anthu okhulupirira monga m'mene mukulakalakalira kapena ngati atatichitira chifundo ndi kutichedwetsera nthawi yathu yokhalira moyo ndi kutikhululukira ku chilango Chake, ndi ndani uyo amene angakutetezeni ndi kukutsekerezani ku chilango chopweteka, chowawa zedi?"

29 Nena: "Iye ndiye (Allah) Wachifundo chambiri, takhulupirira mwa Iye ndiponso kwa iye ndi kumene tatsamira. Posachedwapa mudziwa (chilango chikatsika kuti) ndani (m'magulu awiriwa) ali mu kusokera koonekera".

[Nena: "Allah ndiye Wachifundo chambiri, tamuvomereza Iye ndipo tagwiritsira ntchito malamulo Ake, komanso tamumvera komanso pa Iye Yekhayo tatsamira mu zinthu zathu zonse. Tero muzadziwa inu makafiri chikadzatsika chilango kuti ndi ndani m'magulu awiri mwa ife ndi mwa inu amene ali mukutalikira kowonekeratu kosiya njira yowongoka ya Allah?"

30 Nena: "Tandiuzani ngati madzi anuwa ataphwa (kulowera pansi penipeni); choncho ndani amene angakubweretsereni madzi akasupe?"

[Nena –iwe Mtumiki (SAW) kwa mamushrikina amenewa kuti: "Tandiuzeni ngati madzi anu amene mukumwawa atakhala kuti apita pansi kwambiri moti simukutha kuwafikira mu njira ina ili yonse, ndi ndani wosakhala Allah angakubweretsereni madzi oyenda pamwamba pa nthaka powonekera ndi maso?"]

## (68) SURAT-UL- QALAM

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Nuun. Ndikulumbirira pensulo (imene akulembera angero ndi ena) ndi zimene amalemba.

2 Pa chisomo cha Mbuye wako sindiwe wamisala (pokupatsa uneneri).

3 Ndithu, udzakhala ndi malipiro aakulu osaduka, (onkerankera mtsogolo chifukwa cha mavuto amene ukukumana nawo pofikitsa uthenga).

4 Ndinso ndithu, uli nawo makhalidwe abwino kwambiri (omwe Allah adakulenga nawo).

1,2,3,4 > [Nuun: mawu adatsogola kale zokhudzana ndi zilembo zodukizadukiza pa chiyambi pa Suurat Al-Baqarat. Allah walumbirira pensulo imene amalembera angero komanso anthu ndiponso wazilumbirira zimene iwo amalemba mu zabwino, zothandiza ndi maphunziro. Siuli iwe Mtumiki (SAW) wofooka nzeru kapena wa maganizo ambwerera chifukwa cha mtendere wa Allah umene uli pa

iwe pakukupatsa uneneri ndi utumiki. Ndipo ndithudi uli nawo malipiro aakulu osapunguka kapena kudukiza chifukwa chofikitsa uthenga. Ndipo ndithu iwe Mtumiki (SAW) uli nawo makhalidwe abwino kwambiri awa ndi amene asonkhanitsa Qur'aan mwa makhalidwe abwino koposa. Kudali kuitsatira Qur'aan chifundo chake nkumatsatira lamulo lake ndi kumasiya zomwe ikuletsa.]

5 Basi, posachedwapa uwona, iwonso awona.

6 Kuti ndani mwa inu wamisala (iwe kapena iwo)?

5-6 [Posakhalitsa uwona iwe Mtumiki (SAW) komanso awona makafiri kuti mwandani m'mene muli mayesero ndi misala.]

7 Ndithu, Mbuye wako akumudziwa bwino amene wasokera pa njira Yake;ndiponso akuwadziwa bwino amene ali owongoka.

[Ndithu Mbuye wako Subhaanahu ndi Amene akudziwa bwino kwambiri za munthu woipa amene wapotoka kusiya chipembedzo cha Allah ndi njira ya chiongoko. Komanso ndi amene akudziwa bwino za yemwe ali woona woongoka ku chipembedzo choonadi.]

8 Choncho, usawamvere otsutsa; (usasiye zimene uli nazo ngakhale sakugwirizana nazo).

[Ukhazikike ndi kupitirira pa zomwe iwe Mtumiki (SAW) uli – mu zosemphana nawo anthu okanira ndipo usamawamvere].

9 Akufuna kuti ukadakhala wofewa kwa iwo (pa zinthu zina) nawo akadakhala ofewa (kwa iwe). [Akulakalaka komanso akadakonda iwe ukadamafewetsa nawo ndi kuchitirana nawo pa zina zimene iwo ali pa zimenezo kuti nawo afewe kwa iwe].

10 Ndipo usamumvere aliyense wochulukitsa kulumbira ndiponso woyaluka.

11 Wojeda, woyenda ndi ukazitape (ndi cholinga chowononga umodzi wawo).

12 Wotsekereza zabwino, wamtopola ndipo wamachimo ambiri.

13 Wouma mtima; pamwamba pa izi ndi wodzipachika pa mtundu wa ena (pomwe iye sali m'menemo).

14 Chifukwa choti iye ndi mwini chuma ndi ana (ndi zimene ali kunyadira).

15 Zikawerengedwa kwa iye ayat Zathu amanena: "Izi ndi nthano za akale (ndi zabodza zawo, zopeka).

[Ndipo iwe Mtumiki (SAW) usamumvere munthu aliyense wochulukitsa kulumbira, wabodza, wonyozeka, wojenda anthu, woyenda ndi mijedo nkumakatenga nkhani kwa ena kupititsa kwina chifukwa chofuna kuipitsa pakati pawo. Woumira zedi ndi chuma posiya choonadi. Womanitsitsa kwambiri zabwino. Wopyola malire ake pochita mtopola kwa anthu ndi kulandira zinthu zoletsedwa. Wamachimo ambiri. Wopyola muyeso pa ukafiri wake, woyankhula zonyansa, wotemberedwa. Wodzipachika kwa bambo amene sadamubereke. Ndi chifukwa chakuti iyeyo ndi mwini chuma ndi ana wapyola malire ndi kudzikuza kusiya choonadi. Kukawerengedwa kwa iye imodzi mwa ma ayat a Qur'aan, amawakanira namanena kuti: "Awa ndi mabodza a anthu oyambirira ndi zopeka zawo." Ma ayat amenewa ngakhale adavumbulutsidwa kwa mamushrikina ena monga Al Waliid Bin Al-Mughiirat, kungoti m'menemo muli chenjezo kwa Msilamu kuti asagwirizane naye amene ali ndi mbiri zonyozekazi.]

16 Timuika pa mphuno pake chizindikiro (chosasiyana nacho kuti ayaluke nacho pa maso pa anthu).

[Tidzaika pa mphuno pake chizindikiro chokhazikika choti sangasiyane nacho momulanga iyeyo kuti ayaluke nacho pamaso pa anthu.]

17 Ndithu ife tidawayesa (eni mzinda wa Makka ndi mtendere womwe udali pa iwo, koma adakana monga) momwe tidawayesera eni munda, pamene adalumbira kuti akathyola zipatso za m'munda wawozo m'bandakucha kuti osawuka asawawone (angawapemphe).

18 Ndipo sadapatule (ngakhale wosauka ndi m'modzi yemwe ponena kuti uje timpatse, uje tisampatse, kapena sadanene kuti: "Ngati Allah afuna").

[Ndithudi ife tawayesa anthu a ku Makka powapatsa njala ndi chilala monga m'mene tidawayeserera eni munda pamene adalumbira pakati pawo kuti ndithu akakolola zipatso za munda wawo atalawirira kwambiri kum'mawa kotero sakadya za m'mundamo wosakhala iwo mwa anthu osauka ndi ena ndipo sadanene: "Ngati Allah akufuna".]

19 Mliri woopsa wochokera kwa Mbuye wako udauzinga mundawo iwo ali mtulo.

20 Choncho udakhala ngati wokololedwa (chifukwa cha mliri uja).

[Ndipo Allah adatumiza pa mundawo moto ndi kuuwotcha nthawi ya usiku iwo akugona ndipo udasanduka wopserera, wakuda ngati usiku wa mdima.]

21 Adaitanizana nthawi ya m'bandakucha.

22 "Lawirirani ku munda wanu kuja ngati mukufuna kukolola (kuopera kuti angakuoneni osauka)".

[Ndipo ena adaitana anzawo ena nthawi ya kum'mawa kuti: "Pitani molawiririra ku munda kwanu ngati mwatsimikizadi zokakolola.]

23 Adanyamuka uku akunong'onezana.

24 (Akunena kuti): "Asakulowerereni lero wosauka m'menemo."

[Ndipo adanyamuka mwamsangamsanga uku akunong'onezana za nkhaniyi pakati pawo motere: "Musayerekeze lero kupereka mwayi wolowa m'munda mwanu kwa aliyense mwa anthu osauka"].

25 Ndipo adalawirira ali ndi chitsimikizo choti atha kuwamana (osauka). [Ndipo adayenda kumayambiriro a usana (kum'mawa) kupita ku munda wawo ndi cholinga chachabe powamana zipatso za m'mundamo anthu osauka ali ndi chitsimikizo chonse cha kuthekera kuti zichitikadi zimene alinga m'kuganiza kwawo].

26 Choncho pamene adaona, adanena (uku akunjenjemera): "Ndithu ife tasokera (sikuno ayi, munda wathu uja siuno).

27 "Mwayi, ndiwomwewu koma tamanidwa dzinthu zake".

28 Wolungama mwa iwo adanena: "Kodi sindidakuwuzeni (pamene mudali kulangizana zomana osowa) kuti bwanji osam'kumbukira Allah (ndi kusintha cholinga chanu)".

29 (Iwo) adanena : "Alemekezeke Mbuye wathu, ndithu ife tidali achinyengo (chifukwa chakuipa kwa cholinga chathu).

30 Ndipo adatembenukirana ndikuyamba kudzudzulana.

31 Adati: "E, chionongeko chathu ndithu ife tidapyola malire (mu chinyengo chathu).

32 "Mwina Mbuye wathu angatipatse zabwino m'malo mwa munda wathuwu; ndithu ife tikufunitsitsa kwa Mbuye wathu.

33 (Fanizo la zimene zidaupeza munda) ndi m'mene chimakhalira chilango (Changa chomwe ndimachitsitsa pa dziko lapansi kwa amene chamuyenera); koma chilango cha Tsiku Lomaliza n'chachikulu zedi, akadakhala akudziwa.

26-33 > [Pamene adauwona munda wawo utapserera anaudabwa ndipo adati: "Ndithudi tasokera njira ya ku mundako." Pamene adadziwa kuti umenewo ndiwo munda wawo adati: "Koma kuti ifeyo tamanidwa zabwino zake chifukwa cha chitsimikizo chathu pa umbombo ndi kumana anthu osauka." Adanena wachilungamo wawo kuti: "Kodi sindidakuwuzeni kuti kodi bwanji simukupatula nkunena kuti "Allah akalola?" Iwo pambuyo pobwerera ku kuzindikira kwawo kuti:

سَنَسِمُهُۥ عَلَى ٱلْخُرْطُومِ ﴿١٦﴾ إِنَّا بَلَوْنَٰهُمْ كَمَا بَلَوْنَآ أَصْحَٰبَ ٱلْجَنَّةِ إِذْ أَقْسَمُوا۟
لَيَصْرِمُنَّهَا مُصْبِحِينَ ﴿١٧﴾ وَلَا يَسْتَثْنُونَ ﴿١٨﴾ فَطَافَ عَلَيْهَا طَآئِفٌ مِّن رَّبِّكَ
وَهُمْ نَآئِمُونَ ﴿١٩﴾ فَأَصْبَحَتْ كَٱلصَّرِيمِ ﴿٢٠﴾ فَتَنَادَوْا۟ مُصْبِحِينَ ﴿٢١﴾ أَنِ
ٱغْدُوا۟ عَلَىٰ حَرْثِكُمْ إِن كُنتُمْ صَٰرِمِينَ ﴿٢٢﴾ فَٱنطَلَقُوا۟ وَهُمْ يَتَخَٰفَتُونَ ﴿٢٣﴾
أَن لَّا يَدْخُلَنَّهَا ٱلْيَوْمَ عَلَيْكُم مِّسْكِينٌ ﴿٢٤﴾ وَغَدَوْا۟ عَلَىٰ حَرْدٍ قَٰدِرِينَ ﴿٢٥﴾ فَلَمَّا
رَأَوْهَا قَالُوٓا۟ إِنَّا لَضَآلُّونَ ﴿٢٦﴾ بَلْ نَحْنُ مَحْرُومُونَ ﴿٢٧﴾ قَالَ أَوْسَطُهُمْ أَلَمْ أَقُل
لَّكُمْ لَوْلَا تُسَبِّحُونَ ﴿٢٨﴾ قَالُوا۟ سُبْحَٰنَ رَبِّنَآ إِنَّا كُنَّا ظَٰلِمِينَ ﴿٢٩﴾ فَأَقْبَلَ
بَعْضُهُمْ عَلَىٰ بَعْضٍ يَتَلَٰوَمُونَ ﴿٣٠﴾ قَالُوا۟ يَٰوَيْلَنَآ إِنَّا كُنَّا طَٰغِينَ ﴿٣١﴾ عَسَىٰ
رَبُّنَآ أَن يُبْدِلَنَا خَيْرًا مِّنْهَآ إِنَّآ إِلَىٰ رَبِّنَا رَٰغِبُونَ ﴿٣٢﴾ كَذَٰلِكَ ٱلْعَذَابُ ۖ وَلَعَذَابُ
ٱلْءَاخِرَةِ أَكْبَرُ ۚ لَوْ كَانُوا۟ يَعْلَمُونَ ﴿٣٣﴾ إِنَّ لِلْمُتَّقِينَ عِندَ رَبِّهِمْ جَنَّٰتِ ٱلنَّعِيمِ
﴿٣٤﴾ أَفَنَجْعَلُ ٱلْمُسْلِمِينَ كَٱلْمُجْرِمِينَ ﴿٣٥﴾ مَا لَكُمْ كَيْفَ تَحْكُمُونَ ﴿٣٦﴾ أَمْ
لَكُمْ كِتَٰبٌ فِيهِ تَدْرُسُونَ ﴿٣٧﴾ إِنَّ لَكُمْ فِيهِ لَمَا تَخَيَّرُونَ ﴿٣٨﴾ أَمْ لَكُمْ أَيْمَٰنٌ
عَلَيْنَا بَٰلِغَةٌ إِلَىٰ يَوْمِ ٱلْقِيَٰمَةِ ۙ إِنَّ لَكُمْ لَمَا تَحْكُمُونَ ﴿٣٩﴾ سَلْهُمْ أَيُّهُم
بِذَٰلِكَ زَعِيمٌ ﴿٤٠﴾ أَمْ لَهُمْ شُرَكَآءُ فَلْيَأْتُوا۟ بِشُرَكَآئِهِمْ إِن كَانُوا۟ صَٰدِقِينَ ﴿٤١﴾
يَوْمَ يُكْشَفُ عَن سَاقٍ وَيُدْعَوْنَ إِلَى ٱلسُّجُودِ فَلَا يَسْتَطِيعُونَ ﴿٤٢﴾

"Wayeretsedwa Allah Mbuye wathu ku kupondereza pa zomwe zatipezazi koma kuti ife ndi amene tidali odzipondereza tokha posiya kupatula ndi cholinga chathu chachabe. Ndipo ena mwa iwo adatembenukira kwa anzawo, yense wa iwo akudzudzula mnzake posiya kupatula ndi cholinga chawo choipa. Adati: "O, tsoka lathulo! Ndithudi ife tidali opyola malire pakumana kwathu anthu osowa ndi posemphana kwathu ndi lamulo la Allah, mwina Mbuye wathu nkutipatsa zabwino zoposa munda wathuwu chifukwa cha kulapa kwathu ndi kuzindikira kwa kulakwa kwathu. Ndithu ife kwa Mbuye wathu Yekhayo tikufunitsitsa, tikulakalaka chikhululuko ndi kupempha zabwino." Mofanana ndi chilango chimenecho chimene tidawalnaga nacho eni munda, ndi mmene - chimakhalira chilango Chathu pa dziko lapansi kwa aliyense amene akusemphanitsa malamulo a Allah ndi kuchitira umbombo zimene Allah adampatsa mu mitendere ndipo iye sadapereke m'menemo gawo la Allah. Ndipo ndithu chilango cha Tsiku Lomaliza ndi chachikulu zedi kuposa chilango cha pa dziko lapansi. Akadakhala kuti akuzindikira, bwenzi

ataleka kusiya njira ili yonse imene ingachititse kupeza chilango cha Allah.]

34 Ndithu, oopa Allah adzakhala ndi minda ya mtendere kwa Mbuye wawo. [Ndithu anthu amene awopa chilango cha Allah pochita zimene wawalamulira nazo ndi kusiya zimene wawaletsa, ali nayo kwa Mbuye wawo Tsiku Lomaliza minda momwe muli mtendere wosatha.]

35 Kodi (tisachite chilungamo m'kuweluza Kwathu) tiwayese Asilamu monga anthu ochimwa?

36 Kodi ndi chiyani chakupezani! Nanga mukuweluza bwanji (maweruzo opanda chilungamowa)?

35-36 [Kodi tiwachite anthu odzichepetsa kwa Allah pomumvera ngati makafiri? Mwatani inu kugamula chigamulo chopanda chilungamochi, kotero mwafananiza pakati pawo malipiro?]

37 Kapena muli ndi buku limene mukuwerenga (lochokera kwa Allah limene mkati mwake mwalembedwa kuti):

38 Mudzapeza tsiku limenelo chimene mwachisankha?

37-38 > [Kapena muli nalo buku lomwe lavumbulutsidwa kuchokera kumwamba m'mene mukupezamo kuti womvera ali chimodzimodzi ndi wochimwa, kotero inu mukuwerenga m'menemo zimene mukuyankhulazi? Ndiyeno kuti muli nazo mu buku limenelo zimene mukufuna, mulibetu inu zimenezo].

39 Kapena muli nawo mapangano ndi Ife okafika mpaka Tsiku Lomaliza akuti inu mudzapeza zimene mukudziweluzira?

[Kapena muli nawo mapangano kwa Ife oti ndithu ndithu zidzapezeka kwa inu zimene mukuzifuna ndi kuzilakalaka].

40 Afunse (mamushrikina iwe Muhammad SAW) ndani mwa iwo ali mtsogoleri pa zimenezo?

41 Kodi iwo ali nawo othandizana nawo (pa mawu awa)? Ndipo atabweretsatu othandizana nawo ngatidi akunena zoona.

[Iwe Mtumiki (SAW) afunse mamushrikina kuti: "Ndi ndani wa iwo pa chigamulo chimenecho ali wotsimikizira kuti adzakhala nazo zimenezo? Kapena ali nayo milungu imene ikuwasamalirira iwowo zimene akunenazo ndi kuwathandiza popeza zimene akufunazo, choncho aibweretse ngati akunena zoona mu kudziti kwawo.]

42 (Akumbukire) tsiku la mavuto okhwima, adzaitanidwa (makafiri) kuti achite sijida (polambira Allah) koma sadzatha.

[Tsiku Lakiyama zinthu zidzavuta ndipo mavuto ake adzakulupala ndipo Allah adzabwera kudzaweluza pakati pa zolengedwa ndipo adzavundukula mwendo Wake wolemekezeka womwe siungafanane nawo kanthu kena kalikonse. Adanena Mtumiki (SAW) kuti: "Mbuye wathu adzavundukula mwendo Wake, ndipo adzamuchitira sajdat wokhulupirira aliyense wachimuna kapena wachikazi ndipo adzatsala amene adali kuchita sajdat pa dziko lapansi modzionetsera ndi kufuna kutchuka ndipo adzapita kuti akachite sajdat ndipo udzakhala msana wake chinthu chimodzi (wopanda molumikizira) (Bukhaar,Muslim).]

43 Maso awo adzangoti pansi zyoli, manyazi ndi kunyozeka kudzawaphimba; kumachita kuti adali kuitanidwa (pa dziko lapansi) kuti agwetse nkhope pansi pomwe iwo adali ndi moyo wangwiro (koma ankakana).

[Maso awo atazyolika asakuwanyamula, kutakuta kuyaluka koopsa chifukwa cha chilango cha Allah. Ndithu iwo adali akuitanidwira pa dziko lapansi ku swalaat yochitira Allah ndi kumuchitira Ibaadat iwo ali angwiro oti adakatha kutero ndipo sankagwetsa nkhope zawo pansi chifukwa chodzikuza ndi kudzikweza.]

44 Ndisiire, (iwe Muhammad SAW) ndi amene akukana nkhaniyi tiwakokera ku chilango pang'onopang'ono pamene iwo sakudziwa.

45 Ndipo ndikuwalekerera pochedwetsa chilango; ndithudi makonzedwe Anga ngokhwima, (palibe angapulumuke m'menemo).

[Iwe Mtumiki (SAW) ndisiye ndi anthu amene akuikanira Qur'aan imeneyi, ndithu kwa Ine kuli malipiro awo ndi kuwalanga iwowo. Tiziwapatsa chuma, ana ndi mtendere chifukwa chofuna kuti adzipitiriza machimo kuchokera komwe sakuzindikira kuti zimene zidzakhala chifukwa cha chiwonongeko chawo. Ndipo Ine ndiwalekerera ndi kuwatalikitsira umoyo wawo kuti adzionjezeka machimo. Ndithu chilango Changa kwa eni ukafiri ndi champhamvu kwambiri.]

46 Kapena ukuwapempha malipiro (pofikitsa uthenga) kotero kuti iwo akulemedwa ndi kulipira?

47 Kapena ali nazo (nzeru) zobisika kotero kuti iwo akulemba (zimene akuweluzazo)!

46-47 [Kapena iwe Mtumiki (SAW) ukuwapempha mamushrikana amenewa malipiro a dziko lapansi pofikitsa uthenga kotero iwowo pofunafuna malipiro amenewo akukhala ngati asenzedwa mtolo wolemera? Koma kuti kodi ali nako kuzindikira kwa zinthu zobisika kotero iwo amazilemba kuchokera ku zimenezo zimene akuweluzira nazo kwa eni akewo, zoti ndithudi

iwowo ali ndi ulemerero wopambana kwa Allah kuposa anthu achikhulupiriro?]

(48) Choncho pirira ndi lamulo la Mbuye wako (chifukwa chowalekerera ndi kuchedwetsa chipulumutso chako); ndipo usakhale ngati mwini nsomba (Yunus (AS) pachangu ndi mkwiyo kwa anthu ake) pamene adaitana (Mbuye wake) uku ali wodzazidwa ndi mkwiyo (kupempha kuti chidze mwachangu chilango kwa anthu ake).

(49) Chikadapanda kumufikira chisomo chochokera kwa Mbuye wake (ndi kuvomera kulapa kwake) akadaponyedwa (kuchokera m'mimba mwa chinsomba chija) pagombe (popanda kanthu) ali wodzudzulidwa.

(50) Koma adamusankha Mbuye wake (povomera kulakwa kwake) ndipo adamuchita kukhala m'modzi wa anthu abwino.

48- 50 [Choncho pirira iwe Mtumiki (SAW) pa zomwe walamula Mbuye wako ndi kugamula. Zina mwa zimenezo ndi kuwalekerera makafiriwo komanso kuchedwetsa kukupatsa kupambana pa iwo ndipo usakhale ngati mwini nsomba. Ameneyu ndi Yunusu (AS) mu mkwiyo wake ndi kusapanda kupirira kwake pa anthu ake pamene adaitana Mbuye wake iye ali wodzazidwa ndi mkwiyo akufunitsitsa kufulumira chilango kwa iwo. Chipanda kuti chidam'peza chisomo chochokera kwa Mbuye wake pomupatsa kuthekera kolapa ndikumulandira kulapako bwenzi atabyukulidwa kuchokera m'mimba mwa chinsombacho pa nthaka pa mtetete pa chionongeko, iye akuzinkera zimene akudzudzulidwa nazo. Ndiye Mbuye wake adamusankha za utumiki Wake ndipo adamuchita kukhala m'gulu la anthu olungama amene zitsimikizo , ntchito ndi zoyankhula zawo zidalungama.

(51) Ndithudi anthu amene sadakhulupirire, adayandikira kukutereretsa ndi kunyogodola kwa maso awo (chifukwa cha chidani ndi mkwiyo) pamene adamva chikumbutso ndipo akunena kuti iyeyu ngwamisala.

[Ndithudi adayandikira makafiri pamene adamva Qur'aanyi kuti akupezetse iwe Mtumiki (SAW) mavuto ndi diso lankhwezule chifukwa chakuipidwa kwawo ndi iwe; chipanda chitetezo cha Allah kwa iwe. Ndipo akumanena – malinga ndi zilakolako zawo-kuti iyeyu ndi wamisala.]

(52) Ndipo ichi sichina, koma (ndi phunziro, ndi nzeru) chikumbutso kwa zolengedwa zonse.

[Ndipo Qur'aan sichina koma ulaliki ndi chikumbutso ku zolengedwa zonse mwa anthu komanso ziwanda (majini)].

خَٰشِعَةً أَبۡصَٰرُهُمۡ تَرۡهَقُهُمۡ ذِلَّةٞۖ وَقَدۡ كَانُواْ يُدۡعَوۡنَ إِلَى ٱلسُّجُودِ وَهُمۡ سَٰلِمُونَ
﴿٤٣﴾ فَذَرۡنِي وَمَن يُكَذِّبُ بِهَٰذَا ٱلۡحَدِيثِۖ سَنَسۡتَدۡرِجُهُم مِّنۡ حَيۡثُ
لَا يَعۡلَمُونَ ﴿٤٤﴾ وَأُمۡلِي لَهُمۡۚ إِنَّ كَيۡدِي مَتِينٌ ﴿٤٥﴾ أَمۡ تَسۡـَٔلُهُمۡ أَجۡرٗا فَهُم
مِّن مَّغۡرَمٖ مُّثۡقَلُونَ ﴿٤٦﴾ أَمۡ عِندَهُمُ ٱلۡغَيۡبُ فَهُمۡ يَكۡتُبُونَ ﴿٤٧﴾ فَٱصۡبِرۡ
لِحُكۡمِ رَبِّكَ وَلَا تَكُن كَصَاحِبِ ٱلۡحُوتِ إِذۡ نَادَىٰ وَهُوَ مَكۡظُومٞ ﴿٤٨﴾ لَّوۡلَآ
أَن تَدَٰرَكَهُۥ نِعۡمَةٞ مِّن رَّبِّهِۦ لَنُبِذَ بِٱلۡعَرَآءِ وَهُوَ مَذۡمُومٞ ﴿٤٩﴾ فَٱجۡتَبَٰهُ رَبُّهُۥ
فَجَعَلَهُۥ مِنَ ٱلصَّٰلِحِينَ ﴿٥٠﴾ وَإِن يَكَادُ ٱلَّذِينَ كَفَرُواْ لَيُزۡلِقُونَكَ بِأَبۡصَٰرِهِمۡ
لَمَّا سَمِعُواْ ٱلذِّكۡرَ وَيَقُولُونَ إِنَّهُۥ لَمَجۡنُونٞ ﴿٥١﴾ وَمَا هُوَ إِلَّا ذِكۡرٞ لِّلۡعَٰلَمِينَ ﴿٥٢﴾

ترتيبها ٦٩ — سُورَةُ الحَاقَّةِ — آياتها ٥٢

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

ٱلۡحَآقَّةُ ﴿١﴾ مَا ٱلۡحَآقَّةُ ﴿٢﴾ وَمَآ أَدۡرَىٰكَ مَا ٱلۡحَآقَّةُ ﴿٣﴾ كَذَّبَتۡ ثَمُودُ
وَعَادُۢ بِٱلۡقَارِعَةِ ﴿٤﴾ فَأَمَّا ثَمُودُ فَأُهۡلِكُواْ بِٱلطَّاغِيَةِ ﴿٥﴾ وَأَمَّا
عَادٞ فَأُهۡلِكُواْ بِرِيحٖ صَرۡصَرٍ عَاتِيَةٖ ﴿٦﴾ سَخَّرَهَا عَلَيۡهِمۡ
سَبۡعَ لَيَالٖ وَثَمَٰنِيَةَ أَيَّامٍ حُسُومٗاۖ فَتَرَى ٱلۡقَوۡمَ فِيهَا صَرۡعَىٰ
كَأَنَّهُمۡ أَعۡجَازُ نَخۡلٍ خَاوِيَةٖ ﴿٧﴾ فَهَلۡ تَرَىٰ لَهُم مِّنۢ بَاقِيَةٖ ﴿٨﴾

## (69) SURAT-UL- HAAQQAT

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Chakudza cha choonadi chomwe ndi Kiyama (mwa icho zidzatsimikizika zimene adali kuzikana)

(2) Kodi chakudza cha choona n'chiyani?

(3) Nanga n'chiyani chikudziwitse chakudza cha choonadichi?

1,2,3 > [Kiyama yoti ichitikadi mwachoonadi yomwe pa tsikulo lidzaonekera poyera lonjezo komanso chiopsezo cha mavuto. Kodi Kiyama imene ichitikeyi mchoonadi ndi chiyani mu mbiri zake ndi kakhalidwe kake? Kodi ndi chiyani chimene iwe Mtumiki chikudziwitse ndikukuzindikiritsa zenizeni za Kiyamayo ndi kukupatsa chithunzithunzi cha kuopsa kwake ndi masautso ake?]

(4) Asamudu ndi A'adi adatsutsa za kudza kwa Kiyama (yomwe idzadzidzimutsa zolengedwa mwamphamvu ndi zoopsa zake).

[Asamudu amene ndi anthu a Swaaleh (AS) ndi A'adi amenewo ndi anthu a Huud (AS) adakanira za Kiyama yomwe idzadzidzimutse mitima ndi zoopsa zake.]

وَجَآءَ فِرۡعَوۡنُ وَمَن قَبۡلَهُۥ وَٱلۡمُؤۡتَفِكَٰتُ بِٱلۡخَاطِئَةِ ﴿٩﴾ فَعَصَوۡاْ رَسُولَ
رَبِّهِمۡ فَأَخَذَهُمۡ أَخۡذَةٗ رَّابِيَةً ﴿١٠﴾ إِنَّا لَمَّا طَغَا ٱلۡمَآءُ حَمَلۡنَٰكُمۡ فِي ٱلۡجَارِيَةِ
﴿١١﴾ لِنَجۡعَلَهَا لَكُمۡ تَذۡكِرَةٗ وَتَعِيَهَآ أُذُنٞ وَٰعِيَةٞ ﴿١٢﴾ فَإِذَا نُفِخَ فِي ٱلصُّورِ
نَفۡخَةٞ وَٰحِدَةٞ ﴿١٣﴾ وَحُمِلَتِ ٱلۡأَرۡضُ وَٱلۡجِبَالُ فَدُكَّتَا دَكَّةٗ وَٰحِدَةٗ ﴿١٤﴾
فَيَوۡمَئِذٖ وَقَعَتِ ٱلۡوَاقِعَةُ ﴿١٥﴾ وَٱنشَقَّتِ ٱلسَّمَآءُ فَهِيَ يَوۡمَئِذٖ وَاهِيَةٞ
﴿١٦﴾ وَٱلۡمَلَكُ عَلَىٰٓ أَرۡجَآئِهَاۚ وَيَحۡمِلُ عَرۡشَ رَبِّكَ فَوۡقَهُمۡ يَوۡمَئِذٖ ثَمَٰنِيَةٞ
﴿١٧﴾ يَوۡمَئِذٖ تُعۡرَضُونَ لَا تَخۡفَىٰ مِنكُمۡ خَافِيَةٞ ﴿١٨﴾ فَأَمَّا مَنۡ أُوتِيَ
كِتَٰبَهُۥ بِيَمِينِهِۦ فَيَقُولُ هَآؤُمُ ٱقۡرَءُواْ كِتَٰبِيَهۡ ﴿١٩﴾ إِنِّي ظَنَنتُ أَنِّي مُلَٰقٍ
حِسَابِيَهۡ ﴿٢٠﴾ فَهُوَ فِي عِيشَةٖ رَّاضِيَةٖ ﴿٢١﴾ فِي جَنَّةٍ عَالِيَةٖ ﴿٢٢﴾
قُطُوفُهَا دَانِيَةٞ ﴿٢٣﴾ كُلُواْ وَٱشۡرَبُواْ هَنِيٓـَٔۢا بِمَآ أَسۡلَفۡتُمۡ فِي ٱلۡأَيَّامِ
ٱلۡخَالِيَةِ ﴿٢٤﴾ وَأَمَّا مَنۡ أُوتِيَ كِتَٰبَهُۥ بِشِمَالِهِۦ فَيَقُولُ يَٰلَيۡتَنِي لَمۡ أُوتَ كِتَٰبِيَهۡ
﴿٢٥﴾ وَلَمۡ أَدۡرِ مَا حِسَابِيَهۡ ﴿٢٦﴾ يَٰلَيۡتَهَا كَانَتِ ٱلۡقَاضِيَةَ ﴿٢٧﴾ مَآ أَغۡنَىٰ
عَنِّي مَالِيَهۡۜ ﴿٢٨﴾ هَلَكَ عَنِّي سُلۡطَٰنِيَهۡ ﴿٢٩﴾ خُذُوهُ فَغُلُّوهُ ﴿٣٠﴾ ثُمَّ ٱلۡجَحِيمَ
صَلُّوهُ ﴿٣١﴾ ثُمَّ فِي سِلۡسِلَةٖ ذَرۡعُهَا سَبۡعُونَ ذِرَاعٗا فَٱسۡلُكُوهُ ﴿٣٢﴾ إِنَّهُۥ
كَانَ لَا يُؤۡمِنُ بِٱللَّهِ ٱلۡعَظِيمِ ﴿٣٣﴾ وَلَا يَحُضُّ عَلَىٰ طَعَامِ ٱلۡمِسۡكِينِ ﴿٣٤﴾

(5) Tsono Asamudu adaonongedwa ndi phokoso lopyola muyeso.

(6) Ndipo A'adi adaonongedwa ndi chimphepo chamkuntho, chozizira (champhamvu kwambiri).

(7) Allah adachitumiza kwa iwo pa usiku usanu ndi uwiri ndi masana asanu ndi atatu mowirikiza; kotero ukadawaona ali lambilambi m'menemo ngati mathunthu a mitengo ya kanjedza yopanda kanthu mkati mwake.

(8) Kodi nanga ukumuona wotsala mwa iwo?

5-8 > [Tsono Asamudu ndiye adaonongedwa ndi mkuwo waukulu womwe udapyola malire pa muyezo wake. Ndipo A'adi ndiye adaonongedwa ndi mphepo yozizira kwam'nanu ndi kukuntha kwambiri yomwe adaitumiza Allah kwa iwo mausiku asanu ndi awiri ndi mausana asanu ndi atatu motsatizana,osaleka ngakhalenso kudukiza. Ndipo ukadaona anthu m'mausiku ndi mausana amenewo ali akufa ngati matsinde a mitengo ya kanjedza yowonongeka, yodyeka mkati mwake. Kodi ukuonako za anthu amenewa m'modzi wotsala wosaonongeka?]

(9) Ndipo Farawo ndi amene adalipo iye asadabadwe, ndi khamu la anthu a mizinda yotembenuzidwa (anthu a Loti AS) adadza ndi machimo aakulu.

(10) Ndipo (yense wa iwowa) adanyoza Mtumiki wa Mbuye wawo; choncho adawalanga ndi chilango chopitirira muyezo.

[Ndipo adadza wopyola malireyu ponyoza Farawo ndi amene adadza iye asadabwere mu magulu amene adakanira Atumiki awo komanso anthu a midzi ya anthu a Loti (AS) amene nyumba zawo zidatembenuzidwa pa iwo chifukwa cha mchitidwe wonyansa kuchokera mu ukafiri, kupembedza mafano ndi ziwerewere, kotero gulu lililonse mwa ilo adanyoza Mtumiki wa Mbuye wawo amene adamutumiza kwa iwo. Choncho Allah adawawononga ndi chilango chachikulu.]

(11) Ndithu pamene madzi adasefukira mopyola muyeso (mpaka kumeza mapiri nthawi ya chigumula cha Noah AS), Ife tidakukwezani m'chombo choyandama ndi kuyenda.

(12) Kuti tichichite (chochitikacho chomwe okhulupirira adapulumuka nacho; osakhulupirira naonongeka nacho) kukhala lingaliro ndi phunziro kwa inu, ndikuti lisunge khutu losunga (nkhaniyi).

11-12 [Ndithudi Ife pamene madzi adapyola malire ake kufikira atakwera nakwezeka pamwamba pa chinthu chilichonse, tidanyamula maziko (makolo) anu limodzi ndi Noah (AS) mu chombo chomwe chimayenda pa madzi. Tidatero kuti tichichite chochitikachi chomwe mkati mwake mudali chipumulutso kwa okhulupirira ndi kumizidwa ndi madzi kwa anthu okanira kuti likhale phunziro. Ndiponso kuti khutu lililonse lomwe chikhalidwe chake kusunga zinthu, lisunge zimenezo ndikuti lizindikire za Allah zomwe lamva].

(13) Tsono likadzaimbidwa lipenga, kuimba kumodzi kokha (zamoyo zonse zidzafa),

(14) Ndipo nthaka ndi mapiri nkuchotsedwa m'malo mwake ndi kuphwanyidwa kamodzi kokha,

(15) Tsiku limenelo, chakudza ndiye chidzakhala kuti chadza (imene ili Kiyama chimene chili chimaliziro.

(16) Ndipo thambo lidzasweka, ndipo Tsiku limenelo lidzakhala lofooka (pamene lidali lolimba).

(17) Ndipo Angero adzakhala m'mphepete mwake. Ndipo pamwamba pawo tsiku limenelo (angero) asanu ndi atatu adzasenza Mpando Wachifumu wa Mbuye wawo.

(18) Tsiku limenelo mudzabweretsedwa, sichidzabisika chilichonse chobisika mwa inu.

13-18 [Ndipo mngero adzauzira mu lipenga kuwuzira kumodzi, komwe ndikuuzira

koyamba ndipo ndikumene kudzakhale kuonongeka kwa dziko lonse komanso ndikunyamulidwa nthaka limodzi ndi mapiri kuchoka m'malo mwake ndi kuswedwaswedwa nkuperedwaperedwa kupera kumodzi,pa nthawi imeneyo ndiye kuti Kiyama yadza. Ndipo thambo lidzaswedwa kotero thambolo tsiku limenelo lidzakhala lofooka lawedewede lopanda kugwirika kapena kulimba kulikonse uku angero ali mu mbali mwake ndi mu nsonga zake uku atasenza Mpando Wachifumu wa Mbuye wako, pamwamba pawo Tsiku la Kiyamalo mwa angero akuluakulu asanu ndi atatu. Pa tsiku limenelo mudzaonetsedwa pa maso pa Allah –inu anthu- kuti muwerengedwe zochita zanu komanso kulipidwa, palibe chobisika kwa Iye mu zinsinsi zanu.]

(19) Tsono amene adzapatsidwe kaundula wake chakudzanja lamanja kwake adzanena (mokondwa kwa amene ali mphepete mwake): "Tengani! Werengani kaundula wanga!

(20) "Ndithudi ine ndidatsimikiza (pa dziko lapansi) kuti ndidzakumana ndi chiwerengero changa."

(21) Choncho, iye adzakhala mu moyo wosangalatsa.

(22) M'munda wa pamwamba.

(23) Zipatso zake zoyandikira pansi (zosavuta kuthyola).

(24) (Adzawauza kuti): "Ndipo idyani , imwani mosangalala pa zimene mudatsogoza m'masiku aja adapita."

[Tsono amene adzapatsidwe buku la ntchito zake ndi dzanja lake lamanja, ndiye kuti adzanena mosangalala ndi mokondwa: "Tengani , werengani buku langa, ndithudi ine ndidatsimikiza pa dziko lapansi kuti ndidzapeza malipiro anga Tsiku la Kiyama, kotero ndidalikonzera chikonzero cha chikhulupiriro ndi ntchito zolungama." Kotero iyeyu adzakhala mu umoyo wabwino wosangalala. Mmunda wa mtendere wapamwambamwamba, zipatso zake ndi zoyandikira zoti angazithyole munthu woyimirira, wokhala pansi ndi amene wagona mofanana. Kudzanenedwa kwa iwo kuti: "Idyani mwa mudyo komanso imwani kumwa kotalikitsidwa ku zoipa zilizonse, muli abwinobwino popanda chokupezani choipa chifukwa cha zimene mudazitsogoza mu ntchito zabwino mu masiku amene adapita].

(25) Ndipo amene adzapatsidwe kaundula wake ku dzanja la manzere, adzanena (modandaula): "Kalanga ine! Ndiponi ndidakapanda kupatsidwa kaundula wangayu!

(26) "Nkusadziwa chiwerengero changa!

(27) "Ha! Imfa ija ikadandimaliziratu (ndi kundilekanitsa ine ndi zimenezi).

(28) "Chuma changa sichidandithandize!

(29) "Mphamvu zanga (ndi moyo wanga wathanzi) zandichokera!"

25-29 [Tsono amene adzapatsidwe buku la ntchito zake ndi dzanja lake la manzere ndipo adzanena modandaula ndi mokhumudwa kuti: "Kalanga ine bola ndidakapanda kupatsidwa buku langa, ndipo n'kadapanda kudziwa kuti malipiro anga ngotani! Kalanga ine bola imfa imene ndidafa ija pa dziko lapansi, ikadakhala yoduliratu za ine ndipanda kuwukitsidwa kwa akufa pambuyo pake. Sichidandithandize chuma changa chimene ndidachisonkhanitsa pa dziko lapansi. Chandichokera ine chiwiringulo changa kotero ndiribe choti nkuwiringulira leroli.]

(30) (Kudzanenedwa kwa angero oyang'anira jahena): "M'gwireni ndipo m'njateni (pophatikiza manja ndi khosi)!

(31) "Kenako m'ponyeni ku moto (apse).

(32) "Kenakonso m'lowetseni tcheni lotalika mikwamba makumi asanu ndi awiri (70)!

(33) "Ndithudi iye sadali kukhulupirira mwa Allah wamkulu.

(34) "Sadalinso kulimbikitsa zodyetsa wosauka.

30 – 34 [Kudzanenedwa kwa osunga jahena kuti: "Gwirani woipa, wamachimo ameneyu ndipo muphatikizeni manja ake onse awiri ndi khosi lake ndi magoli kenako mulowetseni m'moto kuti amve kuotcha kwake. Kenakonso mu unyolo wazitsulo kutalika kwake mikwamba makumi asanu ndi awiri ndi kumulowetsa m'menemo. Ndithudi iyeyu sadali kumuvomereza Allah kumachita Iye Yekhayo ndi Wopembedzedwa mwachowonadi wopanda wophatikizana Naye, komanso sanali kugwiritsa ntchito chiongoko Chake komanso sadali kulimbikitsa anthu pa dziko lapansi zodyetsa anthu ovutika m'gulu la osowa ndi ena otero].

(35) "Basi, lero kuno alibe bwenzi (lomuthandiza).

(36) "Ndipo alibe chakudya kupatula mafinya (a anthu a ku moto).

(37) "Zomwe palibe angazidye kupatula ochimwa mwadala"

35-37 [Alibe kafiri ameneyu Tsiku la Kiyama m'bale woti n'kumuchotsera chilango, komanso alibe chakudya kupatula mafinya a anthu a ku moto, sangawadye amenewa kupatula anthu ochimwa amene akupitiriza ukafiri.]

(38) Choncho ndikulumbirira zimene mukuziona,

(39) Ndi zimene simukuziona.

(40) Ndithudi iyi (Qur'aan) ndi liwu la Mthenga Wolemekezeka.

(41) Ndipo simawu a mlakatuli; ndi zochepa

فَلَيْسَ لَهُ الْيَوْمَ هَاهُنَا حَمِيمٌ ﴿٣٥﴾ وَلَا طَعَامٌ إِلَّا مِنْ غِسْلِينٍ ﴿٣٦﴾ لَا يَأْكُلُهُ
إِلَّا الْخَاطِئُونَ ﴿٣٧﴾ فَلَا أُقْسِمُ بِمَا تُبْصِرُونَ ﴿٣٨﴾ وَمَا لَا تُبْصِرُونَ ﴿٣٩﴾
إِنَّهُ لَقَوْلُ رَسُولٍ كَرِيمٍ ﴿٤٠﴾ وَمَا هُوَ بِقَوْلِ شَاعِرٍ قَلِيلًا مَا تُؤْمِنُونَ ﴿٤١﴾
وَلَا بِقَوْلِ كَاهِنٍ قَلِيلًا مَا تَذَكَّرُونَ ﴿٤٢﴾ تَنْزِيلٌ مِنْ رَبِّ الْعَالَمِينَ ﴿٤٣﴾ وَلَوْ
تَقَوَّلَ عَلَيْنَا بَعْضَ الْأَقَاوِيلِ ﴿٤٤﴾ لَأَخَذْنَا مِنْهُ بِالْيَمِينِ ﴿٤٥﴾ ثُمَّ لَقَطَعْنَا
مِنْهُ الْوَتِينَ ﴿٤٦﴾ فَمَا مِنْكُمْ مِنْ أَحَدٍ عَنْهُ حَاجِزِينَ ﴿٤٧﴾ وَإِنَّهُ لَتَذْكِرَةٌ
لِلْمُتَّقِينَ ﴿٤٨﴾ وَإِنَّا لَنَعْلَمُ أَنَّ مِنْكُمْ مُكَذِّبِينَ ﴿٤٩﴾ وَإِنَّهُ لَحَسْرَةٌ عَلَى
الْكَافِرِينَ ﴿٥٠﴾ وَإِنَّهُ لَحَقُّ الْيَقِينِ ﴿٥١﴾ فَسَبِّحْ بِاسْمِ رَبِّكَ الْعَظِيمِ ﴿٥٢﴾

ترتيبها ٧٠ — **سُورَةُ الْمَعَارِجِ** — آياتها ٤٤

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَٰنِ الرَّحِيمِ

سَأَلَ سَائِلٌ بِعَذَابٍ وَاقِعٍ ﴿١﴾ لِلْكَافِرِينَ لَيْسَ لَهُ دَافِعٌ ﴿٢﴾ مِنَ
اللَّهِ ذِي الْمَعَارِجِ ﴿٣﴾ تَعْرُجُ الْمَلَائِكَةُ وَالرُّوحُ إِلَيْهِ فِي
يَوْمٍ كَانَ مِقْدَارُهُ خَمْسِينَ أَلْفَ سَنَةٍ ﴿٤﴾ فَاصْبِرْ صَبْرًا جَمِيلًا ﴿٥﴾
إِنَّهُمْ يَرَوْنَهُ بَعِيدًا ﴿٦﴾ وَنَرَاهُ قَرِيبًا ﴿٧﴾ يَوْمَ تَكُونُ السَّمَاءُ كَالْمُهْلِ
﴿٨﴾ وَتَكُونُ الْجِبَالُ كَالْعِهْنِ ﴿٩﴾ وَلَا يَسْأَلُ حَمِيمٌ حَمِيمًا ﴿١٠﴾

zimene mukuzikhulupirira.
(42) Ndiponso simawu a mlosi;ndi zochepa zimene mumalangizika nazo.
(43) (Ichi ndi ) chivumbulutso chochokera kwa Mbuye wa zolengedwa.

38 – 43 [Ndikulumbirira zimene mukuziona zooneka ndi maso ndi zomwe simukuziona zomwe zabisika kwa inu. Ndithudi Qur'aan imeneyi ndi mawu a Allah amene amawawerenga Mtumiki Wolemekezeka ndi wabwino kwambiri. Ndipo simawu a mlakatuli ngati m'mene mukunenera mwabodza. Ndi zochepa chabe zimene mukuzikhulupirira. Ndipo simawu osanjikizana a mlosi, ndi zochepa zimene zimakhala kwa inu kuganizira ndi kulingalira kusiyana pakati pa ziwirizi. Koma amenewa ndi mawu a Mbuye wa zolengedwa zonse amene adawatumiza kwa Mtumiki Wake Muhammad (SAW).

(44) Ndipo (Mneneri SAW) akadatipekera bodza lililonse."
(45) Tikadam'gwira mwamphamvu,
(46) Ndipo tikadadula mwa iye mtsempha wamoyo (kotero kuti ndikuferatu nthawi yomweyo).
(47) Sipakadapezeka aliyense mwa inu wom'teteza (ku chilango Chathu).
(48) Ndithu iyi (Qur'aan) ndi phunziro kwa oopa (Allah).

44-48 [Akadatipekera Ife Muhammad kanthu kalikonse kamene sitidanene, bwenzi titamugwira ndi dzanjadzanja, kenako ndikumudula mtsempha wa mtima wake, ndipo sadakatha wina aliyense mwa inu kumutsekereza iyeyo ku chilango Chathu. Ndithu Qur'aan imeneyi ndi chikumbutso cha anthu oopa, amene amamvera malamulo a Allah ndi kumapewa zimene waletsa.]

(49) Ndithu Ife, tikudziwa kuti ena mwa inu akutsutsa (Qur'aan).
(50) Ndipo ndithu iyi (Qur'aan) idzakhala chowadandaulitsa (chachikulu) osakhulupirira (pamene adzaona chilango chawo ndi mtendere wa okhulupirira).
(51) Ndithu, (Qur'aan) ndi choonadi chotsimikizika (mulibe chikaiko).
(52) Basi, lemekeza dzina la Mbuye wako Wamkulu (pitiriza kutamanda dzina Lake).

49-52 [Ndithudi Ife tikudziwa kuti mwa inu muli amene akukanira Qur'aan imeneyi angakhale kuti ma ayat ake owonekera poyera. Ndithudi kuikanira Qur'aaniyi ndi dandaulo lalikulu kwa amene amaikanira pa nthawi imene adzaone chilango chawo ndikuonanso chisomo cha anthu oyikhulupirira. Ndithudi Qur'aaniyi ndi choonadi chotsimikizika ndiponso chenicheni chopanda chikaiko mkati mwake. Choncho muyeretse Allah Subhaanahu ku zinthu zosayenerera ndi ulemerero Wake ndipo udzimutchula ndi dzina Lake lalikulu.]

## (70) SUURAT-UL- MAA'RIJ

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Wopempha adapempha kuti chiwadzere msanga chilango chopezekacho (m'kupempha kwa chipongwe ndi kotsutsa).
(2) Kwa okanira chimene palibe angachitsekereze,
(3) Chochokera kwa Allah Mwini makwerero .
(4) Angero ndi Jibril amakwera kwa Iye (Allah), m'tsiku lomwe kutalika kwake kuli ngati zaka zikwi makumi asanu (50,000).

1-4 [Wapempha wopempha mwa ma mushrikina kudzipemphera yekha komanso anthu ake zowatsikira chilango pa iwo, kumachita chilangocho chidzawapeza iwowo Tsiku la Kiyama popanda chipeneko chilichonse. Palibe amene angachitsekereze kwa Allah mwini kupamwamba ndi ulemerero. Angero komanso Jibril adzakwera kwa Iye mu tsiku lomwe lili mulingo wake zaka zikwi makumi asanu (50,000) mu zaka za dziko lapansi, ndipo nyengo

imeneyo kwa munthu wokhulupirira, idzakhala ngati nyengo ya pemphero la faradhwi limodzi.]

(5) Choncho, pirira iwe (Mtumiki SAW) kupirira kwabwino.

[Choncho iwe Mtumiki (SAW) pirirra pa chipongwe chawo ndi kufulumizitsira kwawoko za chilango kupirira kopanda kubabaika mkati mwake komanso kopanda kukadandaulira kwina kosakhala kwa Allah].

(6) Ndithu, iwo akuona (Tsiku la) Kiyama kuti palibe ; silingachitike.

(7) Koma Ife tikuona kuti n'lochitika.

6-7 [Ndithudi makafiri akutalikitsa m'maganizo mwawo kuti palibe chilango ndipo akuliona kuti silingachitike pamene Ife tikuliona kuti ndi lochitikadi, lapafupi popanda chikaiko chilichonse].

(8) Tsiku limene thambo lidzakhala ngati mtovu wosungunuka.

(9) Ndipo mapiri adzakhala ngati ubweya (oluzika).

8-9 [Tsiku limene thambo lidzakhale likuyenda monga ayenderera mafuta owonongeka, ndipo mapiri adzakhala ngati bweya opakidwa utoto wongouluzika ndi mphepo.]

(10) Ndipo m'bale sadzafunsa za m'bale wake,

[Ndipo m'bale sadzafunsa m'bale wake m'mene alili chifukwa choti aliyense wa iwo adzakhala atatanganidwa ndi zake.]

(11) Ngakhale kuti adzawalola kuti awonane ndi kudziwana pakati pawo (koma sadzafunsana). Wochimwa adzalakalaka kuti akadadziombola ku chilango cha tsiku limenelo ndi ana ake.

(12) Mkazi wake, ndi abale ake,

(13) Ndi a ku mtundu wake, amene amam'sunga (ndi kukhala m'modzi wa iwo),

(14) Ndi (kulipira) zonse za m'dziko, kuti zimupulumutse.

11-14 [Adzawaona ndipo adzawazindikira koma sadzatha aliyense kuthandiza mnzake. Adzalakalaka kafiri kuti akadziombole yekha ku chilango cha Tsiku la Kiyama ndi ana ake, mkazi wake, m'bale wake ndi anthu a mtundu wake amene iye akukhudzana naye, ndipo iye akuchokera ku mtunduwo mu ubale komanso ndi onse amene ali pa nthaka mwa anthu kapenanso zolengedwa zina, kenako apulumuke ku chilango cha Allah.]

(15) Iyayi, (siya iwe wamachimo zimene ukulakalakazo) ndithu umenewu ndi moto wa malawi

(16) Wosenda mwamphamvu khungu.

(17) Udzaitana (potchula dzina la aliyense) amene adachitembenuzira msana choona ndi kunyoza.

يُبَصَّرُونَهُمْۚ يَوَدُّ ٱلْمُجْرِمُ لَوْ يَفْتَدِى مِنْ عَذَابِ يَوْمِئِذٍۭ بِبَنِيهِ ﴿١١﴾
وَصَٰحِبَتِهِۦ وَأَخِيهِ ﴿١٢﴾ وَفَصِيلَتِهِ ٱلَّتِى تُـْٔوِيهِ ﴿١٣﴾ وَمَن فِى ٱلْأَرْضِ
جَمِيعًا ثُمَّ يُنجِيهِ ﴿١٤﴾ كَلَّآ ۖ إِنَّهَا لَظَىٰ ﴿١٥﴾ نَزَّاعَةً لِّلشَّوَىٰ ﴿١٦﴾ تَدْعُوا۟
مَنْ أَدْبَرَ وَتَوَلَّىٰ ﴿١٧﴾ وَجَمَعَ فَأَوْعَىٰٓ ﴿١٨﴾ ۞ إِنَّ ٱلْإِنسَٰنَ خُلِقَ هَلُوعًا
﴿١٩﴾ إِذَا مَسَّهُ ٱلشَّرُّ جَزُوعًا ﴿٢٠﴾ وَإِذَا مَسَّهُ ٱلْخَيْرُ مَنُوعًا ﴿٢١﴾ إِلَّا
ٱلْمُصَلِّينَ ﴿٢٢﴾ ٱلَّذِينَ هُمْ عَلَىٰ صَلَاتِهِمْ دَآئِمُونَ ﴿٢٣﴾ وَٱلَّذِينَ فِىٓ
أَمْوَٰلِهِمْ حَقٌّ مَّعْلُومٌ ﴿٢٤﴾ لِّلسَّآئِلِ وَٱلْمَحْرُومِ ﴿٢٥﴾ وَٱلَّذِينَ يُصَدِّقُونَ
بِيَوْمِ ٱلدِّينِ ﴿٢٦﴾ وَٱلَّذِينَ هُم مِّنْ عَذَابِ رَبِّهِم مُّشْفِقُونَ ﴿٢٧﴾ إِنَّ عَذَابَ
رَبِّهِمْ غَيْرُ مَأْمُونٍ ﴿٢٨﴾ وَٱلَّذِينَ هُمْ لِفُرُوجِهِمْ حَٰفِظُونَ ﴿٢٩﴾ إِلَّا عَلَىٰٓ
أَزْوَٰجِهِمْ أَوْ مَا مَلَكَتْ أَيْمَٰنُهُمْ فَإِنَّهُمْ غَيْرُ مَلُومِينَ ﴿٣٠﴾ فَمَنِ ٱبْتَغَىٰ وَرَآءَ
ذَٰلِكَ فَأُو۟لَٰٓئِكَ هُمُ ٱلْعَادُونَ ﴿٣١﴾ وَٱلَّذِينَ هُمْ لِأَمَٰنَٰتِهِمْ وَعَهْدِهِمْ رَٰعُونَ
﴿٣٢﴾ وَٱلَّذِينَ هُم بِشَهَٰدَٰتِهِمْ قَآئِمُونَ ﴿٣٣﴾ وَٱلَّذِينَ هُمْ عَلَىٰ صَلَاتِهِمْ يُحَافِظُونَ
﴿٣٤﴾ أُو۟لَٰٓئِكَ فِى جَنَّٰتٍ مُّكْرَمُونَ ﴿٣٥﴾ فَمَالِ ٱلَّذِينَ كَفَرُوا۟ قِبَلَكَ مُهْطِعِينَ
﴿٣٦﴾ عَنِ ٱلْيَمِينِ وَعَنِ ٱلشِّمَالِ عِزِينَ ﴿٣٧﴾ أَيَطْمَعُ كُلُّ ٱمْرِئٍ مِّنْهُمْ
أَن يُدْخَلَ جَنَّةَ نَعِيمٍ ﴿٣٨﴾ كَلَّآ ۖ إِنَّا خَلَقْنَٰهُم مِّمَّا يَعْلَمُونَ ﴿٣٩﴾

(18) Adasonkhanitsa (chuma) ndi kuchiika (m'nkhokwe zake popanda kuchiperekera chopereka cha Allah).

15-18 [Zinthu sizili monga m'mene ukulakalakalira iwe kafiri mu zodziombolazo ayi, ndithudi imeneyo ndi jahena, moto wake ukuyaka mwamphamvu, chifukwa chakuotcha kwake kwa mphamvu, ukukungunula khungu la m'mutu ndi nsonga za ziwalo zina zonse. Uzidzaitana aliyense amene adachitalikira choonadi pa dziko lapansi ndi kusiya kumumvera Allah ndi Mtumiki Wake (SAW), ndipo adasonkhanitsa chuma nachiika mu nkhokwe zake, ndipo sadaperekere gawo la Allah mu chumacho.]

(19) Ndithu, munthu walengedwa ndi chilengedwe cha kudaida nkhawa (kutekeseka ndi kukwiya),

(20) Mavuto akamukhudza, amada nkhawa.

(21) Koma zabwino zikam'khudza, amamana (ena ndi kuiwala mavuto amene adali nawo).

(22) Kupatula opemphera (iwo alibe mbiri zoipazi).

(23) Iwo amene akupitiriza mapemphero awo (sakuwaleka ngakhale zivute chotani).

(24) Ndi iwo amene m'chuma chawo muli gawo lodziwika,

25 La wopempha chithandizo ndi omanidwa (amene sapemphapempha chifukwa chodzisungira ulemu wake)

26 Ndi amene akuvomereza za Tsiku Lachiweruzo (ndi kumalikonzekera).

27 Ndi iwo amene akuopa chilango chochokera kwa Mbuye wawo,

28 Ndithu, chilango cha Mbuye wawo n'chosapulumuka nacho (munthu woipa).

29 Ndiponso iwo amene akusunga umaliseche wawo (posachita chiwerewere),

30 Kupatula kwa akazi awo ndi amene manja awo akumanja apeza; ndithu pa zimenezo iwo sangadzudzulidwe.

19-30 [Ndithu munthu adalengedwa kukhala wotaya mtima ndi khama lalikulu. Chikampeza choipa ndi sautso, iye amachulukitsa kutaya mtima ndi kudandaula. Ndipo ngati chabwino ndi chofewa chamupeza, ndiyeno amachulukitsa kumana komanso kuumira. Kupatula amene ali opemphera mwadongosolo, amene amasunga zowapemphera mapempherowa nthawi zonse ndipo palibe china chowatangwanitsa. Komanso anthu amene mu chuma chawo muli gawo lodziwika limene Allah adawalamulira kuti adzilipereka, imeneyo ndiyo Zakaat, kuti adziipereka kwa amene wawapempha chithandizo komanso amene wadzitsekereza kutero. Ndiponso ndi anthu amene akukhulupirira tsiku lowerengeredwa malipiro, ndi kumalikonzekera ndi ntchito zabwino. Komanso ndi anthu amene akuopa chilango cha Allah. Ndithu chilango cha Mbuye wawo nkosafunika kwa wina aliyense kudziika pa chitetezo kuti sichikam'khudza. Komanso anthu amene maliseche awo ali owasunga ku zilizonse zimene Allah wawaletsa, kupatula kwa akazi awo ndi adzakazi awo, iwowa sangalangidwe nawo.}

31 Koma amene angafune (zosangalatsa) kusiya zimenezo, iwowo ndiwo olumpha malire.

32 Ndi iwo amene amasunga mwaubwino zimene amasungitsidwa ndi zimene alonjeza (Allah ndi anthu),

33 Ndi iwo amene amaima molungama popereka maumboni awo,

34 Ndiponso iwo amene amasunga (mwa ubwino) mapemphero awo,

35 Amene ali ndi mbiri zimenezi adzakhala m'minda (ya mtendere) ali olemekezedwa.

[Ndipo amene angafune kukwaniritsa chilakolako chake kosakhala kwa akazi ake ndi adzakazi, ndiye kuti iwowo ndi odumpha malire a zinthu zovomerezeka, kuchita zoletsedwa. Ndiponso anthu amene akusamala bwino zimene asungitsidwa ndi Allah komanso akapolo (anthu anzawo), komanso osunga mapangano awo ndi Allah komanso akapolo (anthu). Ndi anthu amene amapereka maumboni awo mwa choonadi mopanda kutembenuza kapena kubisa. Komanso anthu amene akusunga zochita mapemphero (Swalaat) ndipo sasiya kalikonse mu zomwe zakakamizidwa za Swalaatyo. Iwowo amene ali ndi mbiri za pamwamba zoterowo, akakhazikika mu minda ya mtendere, akalemekezedwa m'menemo ndi mtundu uli wonse m'mitundu ya ulemerero.]

36 Kodi kuli chiyani kwa amene akana (makafiri) akuthamangira kwa iwe (maso ali pa mtunda)

37 (Atakuzungulira) ena chakumanja ena cha kumanzere m'magulumagulu.

38 Kodi akulakalaka aliyense mwa iwo kuti akalowetsedwe ku munda wa mtendere.

39 Asiye (kukhumba kwawo kokalowa ku munda wa mtendere)! Ndithu, ife tidawalenga kuchokera m'zimene akudziwa (madzi opanda pake).

36-39 [Kodi ndi chinthu chanji chawachititsa makafiri amenewa kuti ayende kulunjika komwe iwe Mtumiki (SAW) uli mofulumira, iwo ataongola makosi awo kwa iwe ataloza maso awo pa iwe akusonkhana ku manja kwako ndi kumanzere kwako ali magulumagulu ochuluka, komanso makamumakamu osiyanasiyana akukambirana komanso kumadabwa? Kodi akulakalaka aliyense wa makafiri amenewa kuti Allah akamulowetsa m'munda wa mtendere wosatha? Zinthu sizili momwe akulakalakaliramo ayi, ndithudi iwowo sakawulowa mundawo mpaka kalekale. Ndithu Ife tidawalenga iwowo kuchokera mu zinthu zimene akuzidziwa kuchokera ku madzi opanda pake monga umo tidachitira ndi ena osakhala iwo, ndipo iwo sadakhulupirire ndiye motani akalemekezedwe ndi kukalowa ku munda wa mtendere?]

40 Ndikulumbirira Mbuye wa kuvuma konse ndi kuzambwe konse, ndithu Ife ndi Okhoza (kuchita chilichonse).

41 Kuwasintha ndi kudzetsa abwino kuposa iwo. Ife palibe (chilichonse) chotipambana.

40 -41[Ndikulumbirira Mbuye wa kotulukira dzuwa konse ndi nyenyezi komanso wa kolowera konse, ndithudi Ife ndi Wokhoza kusintha m'malo mwa iwowo kubwereretsa anthu ena abwino kuposa iwo komanso omvera kwambiri Allah. Ndipo palibe wina aliyense amene angatitsogolere , kutiposa kapena kutilepheretsa titafuna kuti timubwezeretse.]

42 Asiye azingolankhula zopanda pake ndi

فَلَآ أُقۡسِمُ بِرَبِّ ٱلۡمَشَٰرِقِ وَٱلۡمَغَٰرِبِ إِنَّا لَقَٰدِرُونَ ﴿٤٠﴾ عَلَىٰٓ أَن نُّبَدِّلَ خَيۡرٗا مِّنۡهُمۡ
وَمَا نَحۡنُ بِمَسۡبُوقِينَ ﴿٤١﴾ فَذَرۡهُمۡ يَخُوضُواْ وَيَلۡعَبُواْ حَتَّىٰ يُلَٰقُواْ يَوۡمَهُمُ ٱلَّذِي
يُوعَدُونَ ﴿٤٢﴾ يَوۡمَ يَخۡرُجُونَ مِنَ ٱلۡأَجۡدَاثِ سِرَاعٗا كَأَنَّهُمۡ إِلَىٰ نُصُبٖ يُوفِضُونَ
﴿٤٣﴾ خَٰشِعَةً أَبۡصَٰرُهُمۡ تَرۡهَقُهُمۡ ذِلَّةٞۚ ذَٰلِكَ ٱلۡيَوۡمُ ٱلَّذِي كَانُواْ يُوعَدُونَ ﴿٤٤﴾

## سُورَةُ نُوحٍ

ترتيبها ٧١ — آياتها ٢٨

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

إِنَّآ أَرۡسَلۡنَا نُوحًا إِلَىٰ قَوۡمِهِۦٓ أَنۡ أَنذِرۡ قَوۡمَكَ مِن قَبۡلِ أَن يَأۡتِيَهُمۡ
عَذَابٌ أَلِيمٞ ﴿١﴾ قَالَ يَٰقَوۡمِ إِنِّي لَكُمۡ نَذِيرٞ مُّبِينٌ ﴿٢﴾ أَنِ ٱعۡبُدُواْ
ٱللَّهَ وَٱتَّقُوهُ وَأَطِيعُونِ ﴿٣﴾ يَغۡفِرۡ لَكُم مِّن ذُنُوبِكُمۡ وَيُؤَخِّرۡكُمۡ
إِلَىٰٓ أَجَلٖ مُّسَمًّىۚ إِنَّ أَجَلَ ٱللَّهِ إِذَا جَآءَ لَا يُؤَخَّرُۚ لَوۡ كُنتُمۡ تَعۡلَمُونَ
﴿٤﴾ قَالَ رَبِّ إِنِّي دَعَوۡتُ قَوۡمِي لَيۡلٗا وَنَهَارٗا ﴿٥﴾ فَلَمۡ يَزِدۡهُمۡ دُعَآءِيٓ إِلَّا
فِرَارٗا ﴿٦﴾ وَإِنِّي كُلَّمَا دَعَوۡتُهُمۡ لِتَغۡفِرَ لَهُمۡ جَعَلُوٓاْ أَصَٰبِعَهُمۡ
فِيٓ ءَاذَانِهِمۡ وَٱسۡتَغۡشَوۡاْ ثِيَابَهُمۡ وَأَصَرُّواْ وَٱسۡتَكۡبَرُواْ ٱسۡتِكۡبَارٗا
﴿٧﴾ ثُمَّ إِنِّي دَعَوۡتُهُمۡ جِهَارٗا ﴿٨﴾ ثُمَّ إِنِّيٓ أَعۡلَنتُ لَهُمۡ وَأَسۡرَرۡتُ
لَهُمۡ إِسۡرَارٗا ﴿٩﴾ فَقُلۡتُ ٱسۡتَغۡفِرُواْ رَبَّكُمۡ إِنَّهُۥ كَانَ غَفَّارٗا ﴿١٠﴾

kumangosewera mpaka adzakumana ndi tsiku lawo limene akulonjezedwa.

(43) Tsiku limene adzatuluke m'manda uku akuthamanga (kudza kwa woitana) ngati kuti akuthamangira ku mafano awo (a miyala amene adali kuwapembedza).

(44) Maso awo ali zyoli (osatha kuwakweza), kuyaluka kutawaphimba. Limenelo ndilo tsiku lomwe adali kulonjezedwa (pomwe adali pa dziko lapansi).

42-44 [Asiye amenewo adzingolowerera mu zabodza zawozo ndipo adzingosewera mu za dziko lapansi lawoli kufikira pamene adzakumane nalo Tsiku la Kiyama limene akulonjezedwa m'menemo ndi chilango. Tsiku limene adzatuluke kuchokera m'manda mofulumira monga m'mene adalili pa dziko lapansi akupita ku milungu yawo yomwe adadzipangira kuti adziyipembedza kusiya Allah. Azidzathamanga ndi kumafulumira maso awo ali onyozeka atazyolikira pansi. Kuyaluka ndi kupeputsidwa kutawaphimba. Tsiku limenelo ndi limene adalonjezedwa nalo pa dziko lapansi ndipo adali kulichitira chibwana ndi kulikanira.

# (71) SUURAT NUH

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Ndithu Ife tidamutuma Nuh kwa anthu ake, (ndikumuuza kuti) : "Chenjeza anthu ako chisadawafike chilango chowawa".

(2) Adanena (Nuh): "E, inu anthu anga! Ndithu, ine ndi mchenjezi kwa inu wowonekera poyera (wolongosola za uthenga wa Mbuye wanu m'chiyankhulo chimene mukuchidziwa).

(3) "M'pembedzeni Allah, ndipo muopeni (posiya zoletsedwa) ndikutinso mundimvere (pa zimene ndikukulangizani)

(4) "(Ngati mutero) adzakukhululukirani machimo anu ndi kutalikitsa moyo wanu kufikira m'nthawi imene yaikidwa (kuti ndiwo malire akutalika kwa moyo). Ndithu nthawi ya Allah ikabwera siichedwerera (ngakhale pang'ono). Mukadakhala mukudziwa (madandaulo omwe mudzakhale nawo imfa ikakufikani, mukadakhulupirira)".

1- 4 [Ndithu ife tidam'tumiza Nuh kwa anthu ake ndipo tidati kwa iye: "Achenjeze anthu ako chisadafikire chilango chowawitsa". Nuh (AS) adati: "E, inu anthu anga! Ndithudi ine ndi mchenjezi wanu woonekera, chenjezo lake la chilango cha Allah ngati mutamunyoza, ndiponso ndikuti ine ndi Mtumiki wa Allah kwa inu, choncho mupembedzeni Iye Yekhayo ndipo opani chilango Chake, komanso ndimvereni ine mu zimene ndikukulamulani ndi zomwe ndikukuletsani kuzichita. Ngati mutandimvera ine ndi kundivomereza, Allah akufafanizirani machimo anu ndi kukukhululukirani. Komanso akutalikitsirani moyo wanu kufikira mu nyengo imene idalinganizidwira mu kuzindikira kwa Allah. Ndithu imfa ikabwera simachedwerera ngakhale pang'ono. Mukadakhala mukudziwa zimenezo bwenzi mutafulumizitsira za chikhulupiriro ndi kumvera".]

(5) Adanena (Nuh): "Ambuye! Ine ndaitanira anthu anga (ku chikhulupiriro) usiku ndi usana (popanda kufooka)

(6) "Kuitana kwanga sikudaonjezere (chilichonse) koma kuthawa basi (ku chikhulupirio Chanu).

(7) "Ndipo ine nthawi iliyonse ndikawaitanira (ku chikhulupiriro Chanu) kuti mwakhululukire, akuika zala zawo m'makutu mwawo (kuti asamve uthenga Wanu), ndipo akudziphimba ndi nsalu zawo (kuti asaone nkhope yanga), ndipo akupitiriza kukana kwawo ndi kudzikweza kwakukulu.

(8) "Kenaka ine ndawaitanira ndi mawu ofuula.

(9) "Kenakanso ine ndawaitanira molengeza poyera ndiponso mwachinsinsi mobisa.

(10) "Ndidati (kwa anthu anga): pemphani kwa Mbuye wanu chikhululuko (pa kukana kwanu

يُرْسِلِ ٱلسَّمَآءَ عَلَيْكُم مِّدْرَارًا ﴿١١﴾ وَيُمْدِدْكُم بِأَمْوَٰلٍ وَبَنِينَ وَيَجْعَل
لَّكُمْ جَنَّٰتٍ وَيَجْعَل لَّكُمْ أَنْهَٰرًا ﴿١٢﴾ مَّا لَكُمْ لَا تَرْجُونَ لِلَّهِ وَقَارًا ﴿١٣﴾
وَقَدْ خَلَقَكُمْ أَطْوَارًا ﴿١٤﴾ أَلَمْ تَرَوْا۟ كَيْفَ خَلَقَ ٱللَّهُ سَبْعَ سَمَٰوَٰتٍ
طِبَاقًا ﴿١٥﴾ وَجَعَلَ ٱلْقَمَرَ فِيهِنَّ نُورًا وَجَعَلَ ٱلشَّمْسَ سِرَاجًا ﴿١٦﴾
وَٱللَّهُ أَنۢبَتَكُم مِّنَ ٱلْأَرْضِ نَبَاتًا ﴿١٧﴾ ثُمَّ يُعِيدُكُمْ فِيهَا وَيُخْرِجُكُمْ
إِخْرَاجًا ﴿١٨﴾ وَٱللَّهُ جَعَلَ لَكُمُ ٱلْأَرْضَ بِسَاطًا ﴿١٩﴾ لِّتَسْلُكُوا۟ مِنْهَا
سُبُلًا فِجَاجًا ﴿٢٠﴾ قَالَ نُوحٌ رَّبِّ إِنَّهُمْ عَصَوْنِى وَٱتَّبَعُوا۟ مَن لَّمْ يَزِدْهُ
مَالُهُۥ وَوَلَدُهُۥٓ إِلَّا خَسَارًا ﴿٢١﴾ وَمَكَرُوا۟ مَكْرًا كُبَّارًا ﴿٢٢﴾ وَقَالُوا۟
لَا تَذَرُنَّ ءَالِهَتَكُمْ وَلَا تَذَرُنَّ وَدًّا وَلَا سُوَاعًا وَلَا يَغُوثَ وَيَعُوقَ
وَنَسْرًا ﴿٢٣﴾ وَقَدْ أَضَلُّوا۟ كَثِيرًا ۖ وَلَا تَزِدِ ٱلظَّٰلِمِينَ إِلَّا ضَلَٰلًا ﴿٢٤﴾
مِّمَّا خَطِيٓـَٰٔتِهِمْ أُغْرِقُوا۟ فَأُدْخِلُوا۟ نَارًا فَلَمْ يَجِدُوا۟ لَهُم مِّن دُونِ
ٱللَّهِ أَنصَارًا ﴿٢٥﴾ وَقَالَ نُوحٌ رَّبِّ لَا تَذَرْ عَلَى ٱلْأَرْضِ مِنَ ٱلْكَٰفِرِينَ
دَيَّارًا ﴿٢٦﴾ إِنَّكَ إِن تَذَرْهُمْ يُضِلُّوا۟ عِبَادَكَ وَلَا يَلِدُوٓا۟ إِلَّا فَاجِرًا
كَفَّارًا ﴿٢٧﴾ رَّبِّ ٱغْفِرْ لِى وَلِوَٰلِدَىَّ وَلِمَن دَخَلَ بَيْتِىَ
مُؤْمِنًا وَلِلْمُؤْمِنِينَ وَٱلْمُؤْمِنَٰتِ وَلَا تَزِدِ ٱلظَّٰلِمِينَ إِلَّا تَبَارًۢا ﴿٢٨﴾

ndi kutonza kwanu). Ndithu, Iye sadasiye kukhala Wokhululuka (machimo kwa amene akubwerera kwa Iye).

5-10 [Nuh (AS) adati: "Mbuye wanga, ine ndaitanira anthu anga ku chikhulupiriro cha Inu ndi ku kukumverani mu usiku ndi usana, koma kuwaitanira kwanga iwo ku chikhulupiriro, sikudaonjezere kalikonse kupatula kuthawa ndi kusalabadira. Ndipo ndithu nthawi zonse ndikawaitanira ku chikhulupiriro mwa Inu, kuti chikhale chifukwa cha chikhululuko Chanu cha machimo awo, akumaika zala zawo m'makutu mwawo kuti asamve kuitanira kwa choonadi. Komanso akumadziphimba ndi nsalu zawo kuti asamandione. Ndipo apitirira pa ukafiri wawo, ndipo adzikweza kusiya kulandira chikhulupiriro kudzikweza kwam'nanu. Kenaka ine ndawaitanira ku chikhulupiriro mowonekera poyera mopanda kubisa, kenakanso ndithu ine ndawonetsera poyera kuitanira iwo ndi mawu okweza, nthawi zina, ndipo nthawi zinanso, ndimawaitanira mwa chinsinsi. Ndipo ndimanena kwa anthu anga kuti: "Mupempheni Allah chikhululuko cha machimo anu ndipo lapani kwa Iye posiya ukafiri wanu, ndithu Iyeyo Wapamwambamwamba ndi wokhululukira amene walapa mwa akapolo Ake ndi kubwerera kwa Iye.]

(11) "Akutumizirani mvula yotsika mochuluka.

(12) "Ndikukupatsani chuma ndi ana (zomwe ndi zokongoletsa za dziko lapansi), ndi kukupangirani mitsinje (yothirira mbewu zanu ndi kumwetsa ziweto zanu).

(13) "Kodi chifukwa chiyani simupereka ulemu kwa Allah (woyenerera ulemerero Wake kuti akakuchitireni chifundo ndi kukupulumutsani ku chilango).

(14) "Pomwe Iye adakulengani m'njira zosiyanasiyana (madzi a umunthu, kenako magazi, kenako magazi ochindikala, kenako mafupa ndipo kenako m'nofu).

(15) "Kodi simudaone momwe Allah adalengera thambo zisanu ndi ziwiri mosanjikana?

(16) "Ndi kupanga mwezi m'thambomo kukhala kuunika, ndiponso kulipanga dzuwa kukhala nyali?

11-12 [Ngati mutalapa ndikupempha chikhululuko, Allah akutsitsirani inuyo mvula yambiri mowirikiza. Ndipo akuchulukitsirani chuma chanu ndi ana anu, komanso akupangirani minda inu nkumasangalala ndi zipatso zake ndi kukongola kwake, ndiponso akuchitirani mitsinje yomathiririra ndi imeneyo mbewu zanu komanso kumwetsa ziweto zanu. Bwanji inu anthu simuopa ukulu wa Allah ndi ufumu Wake, kumachita kuti adakulengani mu nyengo zosiyanasiyana motere: umuna, kenako magazi wochindikala kenako mnofu kenako mafupa kenako nyama? Kodi simukuona m'mene walengera Allah mitambo isanu ndi iwiri mosanjikana lina pamwamba pa linzake, ndipo adauchita mwezi m'mitambo imeneyo kukhala dangalira, nalichita dzuwa kukhala nyali yowala yomapezera kuwala anthu a pa dziko lapansi?]

(17) "Ndipo Allah adakulengani kuchokera m'nthaka monga m'mera.

(18) "Kenako adzakubwezerani momweno (mutafa) ndi kudzakutulutsaninso (popanda cholepheretsa).

(19) "Ndipo Allah wakupangirani nthaka kukhala ngati choyala,

(20) "Kuti muziyendayenda m'menemo m'njira zazikulu."

17-20 [Ndipo Allah adalipanga tsinde lanu kuchokera mu nthaka mokulinganizani kenako amakubwezeretsani mu nthakamo pambuyo pa imfa ndipo adzakutulutsani kuchokera m'menemo tsiku louka kwa akufa kukutulutsani kwachoonadi. Ndipo Allah adakuchitirani nthaka kukhala yotambasuka

ngati choyala kuti muthe kumayendapo mu njira zikuluzikulu].
21 Adanena Nuh (AS): "Ambuye! Ndithu anthu anga andinyoza (pa zimene ndawalamula kuti akhulupirire Inu ndi kupempha chikhululuko Chanu, ndipo (ofooka mwa iwo) am'tsatira yemwe chuma chake ndi ana ake sizidzamuonjezera (chilichonse chabwino) koma kutaika (ndi kuonongeka pa Tsiku Lomaliza).
22 "Ndipo (eni chuma ndi ana) awatchera otsatira awo ndale zazikulu (zopyola muyeso kuti asakhulupirire).
23 "Ndipo adanena (kwa otsatira awo) : "Musasiye kupembedza milungu yanu; musasiye Wadda, Suwaa, Yaghuutha, Ya'uka ndi Nasra (maina a mafano awo).
24 "Ndipo ndithu iwo asokeretsa (anthu) ambiri ndipo musawaonjezere ochita zoipa (china chake) koma kusokera basi ndi kukhala kutali ndi choonadi".
25 Chifukwa cha zochimwa zawo, adamizidwa ndi kulowetsedwa ku moto (waukulu,woyaka) ndipo sadapeze owapulumutsa ndi kuwateteza m'malo mwa Allah.
21-25 [Nuh (AS) adati: "Mbuye wanga! Ndithu anthu anga apyola malire ponyoza ine ndi kundikanira. Ndipo ofooka mwa iwo atsatira atsogoleri osokeretsa amene chuma chawo ndi ana awo sadawaonjezere kalikonse kupatula kusokera pa dziko lapansi ndi kukapeza chilango Tsiku Lomaliza. Ndipo atsogoleri a chisokero awatchera ndale owatsatira awo mwa anthu ofooka ndale zazikulu ndipo anena kwa iwowo kuti: "Musasiye kupembedza milungu yanu kuti mudzipembedza Allah Yekhayo Yemwe akuitanira kwa Iye Nuh (AS) ayi. Ndipo musamusiye Wadda, Suwa'a, Yaghuutha, Yau'uka ndi Nasra- amenewa ndi maina a mafano awo amene adali kuwapembedza kusiya Allah. Ndipo adali maina a anthu olungama, pamene adafa satana adanong'oneza anthu awo kuti awaimikire mafano ndi zithunzi ati ponama kwawo kuti akhale ndi mphamvu pomvera akaona zithunzizo. Pamene anthu amenewa adachoka, nkutalika nthawi, ndi kulowa m'malo mwawo anthu ena osakhala iwo, satana adawanong'oneza kuti amene adatsogola a iwo adali kupembedza mafano ndi zithunzi zimenezo ndipo adali kupempha kudzera mwa izo. Ichi ndicho cholinga chimene kudaletseredwera mafano ndi kuletsa kumanga ziriza pa manda chifukwa ndi kutalika kwa nthawi zidzakhala zopembedzedwa kwa ambuli. Ndithu adasokeretsa awa otsatidwawa anthu ambiri ndi zomwe adazikongoletsa kwa iwo mu njira za chisokonekero. Kenako Nuh (AS) adati: "Kotero inu Mbuye wathu musaonjezere awa odzipondereza okhawa ndi ukafiri ndi mwano ndi kena kalikonse kupatula kutalikira ku choonadi. Ndipo chifukwa cha machimo awo ndi liuma lawo pa ukafiri ndi kupyola malire, adamizidwa ndi chikumba cha madzi, kenako adalowetsedwa pambuyo pomizidwa kwawoko ku muto woyaka kwambiri malawi ake ndi kuotcha ndipo sadapeze wina wake wosakhala Allah wowathandiza kapena kwatchinjiriza ku chilango cha Allah.]
26 Ndipo adanena Nuh (AS) (atataya mtima za anthu ake): "Ambuye! Musasiye aliyense mwa osakhulupirira kukhala pa dziko.
27 "Ndithu Inu Ambuye ngati muwasiya (popanda kuwaononga) asokeretsa akapolo Anu (ku njira yolungama). Ndipo sangabereke (ana abwino) koma oipa; osakhulupirira (okhala kutali ndi choonadi, ndiponso onyoza Inu).
28 "Mbuye wanga! Ndikhululukireni ine ndi makolo anga, ndi aliyense walowa m'nyumba yanga ali wokhulupirira ndi okhulupirira aamuna ndi okhulupirira aakazi. Ndipo musawaonjezere anthu opondereza chinachake koma kuwaononga basi".
25-28 [Ndipo Nuh (AS) pambuyo potaya mtima kuchokera mu kumva kwake anati: "Mbuye wanga! Musasiye aliyense mu anthu okanira Inu wina aliyense wamoyo pa dziko lapansi woti nkumazungulirazungulira nkumatekeseka pa dziko lapansi. Ndithu Inu ngati muwasiye popanda kuwaononga, adzasokeretsa akapolo Anu amene adakukhulupirirani Inu ku njira ya choonadi ndipo sangabwere kuchokera ku misana yawo kapena mu ziberekero zawo kupatula opotoka kusiya choonadi, wokanira kwambiri ndi kunyoza Inu. Mbuye wanga! Ndikhululukireni ine ndi makolo anga ndi omwe amene alowa m'nyumba yanga ali wokhulupirira, komanso akhululukireni anthu okhulupirirra mwa Inu achimuna ndi achikazi omwe, koma musawaonjezere anthu okanirawa kupatula kuonongeka ndi kutaika pa dziko lapansi lino ndi Tsiku Lomaliza.]

## (72) SURAT-UL- JINN

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Nena (iwe Mtumiki SAW kwa anthu): "Allah wavumbulutsa kwa ine kuti gulu la ziwanda lidamvetsera (kuwerenga kwanga Qur'aan) ndipo lidanena (ku mtundu wawo), ndithu, tamvetsera Qur'aan yodabwitsa (sitiidamvere yonga iyi chiyambire).

ترتيبها ٧٢ — سُورَةُ الجِنِّ — آياتها ٢٨

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَٰنِ الرَّحِيمِ

قُلْ أُوحِيَ إِلَيَّ أَنَّهُ اسْتَمَعَ نَفَرٌ مِّنَ الْجِنِّ فَقَالُوا إِنَّا سَمِعْنَا قُرْآنًا
عَجَبًا ﴿١﴾ يَهْدِي إِلَى الرُّشْدِ فَآمَنَّا بِهِ ۖ وَلَن نُّشْرِكَ بِرَبِّنَا أَحَدًا ﴿٢﴾
وَأَنَّهُ تَعَالَىٰ جَدُّ رَبِّنَا مَا اتَّخَذَ صَاحِبَةً وَلَا وَلَدًا ﴿٣﴾ وَأَنَّهُ كَانَ
يَقُولُ سَفِيهُنَا عَلَى اللَّهِ شَطَطًا ﴿٤﴾ وَأَنَّا ظَنَنَّا أَن لَّن تَقُولَ الْإِنسُ
وَالْجِنُّ عَلَى اللَّهِ كَذِبًا ﴿٥﴾ وَأَنَّهُ كَانَ رِجَالٌ مِّنَ الْإِنسِ يَعُوذُونَ بِرِجَالٍ
مِّنَ الْجِنِّ فَزَادُوهُمْ رَهَقًا ﴿٦﴾ وَأَنَّهُمْ ظَنُّوا كَمَا ظَنَنتُمْ أَن لَّن يَبْعَثَ
اللَّهُ أَحَدًا ﴿٧﴾ وَأَنَّا لَمَسْنَا السَّمَاءَ فَوَجَدْنَاهَا مُلِئَتْ حَرَسًا
شَدِيدًا وَشُهُبًا ﴿٨﴾ وَأَنَّا كُنَّا نَقْعُدُ مِنْهَا مَقَاعِدَ لِلسَّمْعِ ۖ فَمَن
يَسْتَمِعِ الْآنَ يَجِدْ لَهُ شِهَابًا رَّصَدًا ﴿٩﴾ وَأَنَّا لَا نَدْرِي أَشَرٌّ أُرِيدَ
بِمَن فِي الْأَرْضِ أَمْ أَرَادَ بِهِمْ رَبُّهُمْ رَشَدًا ﴿١٠﴾ وَأَنَّا مِنَّا الصَّالِحُونَ
وَمِنَّا دُونَ ذَٰلِكَ ۖ كُنَّا طَرَائِقَ قِدَدًا ﴿١١﴾ وَأَنَّا ظَنَنَّا أَن لَّن نُّعْجِزَ
اللَّهَ فِي الْأَرْضِ وَلَن نُّعْجِزَهُ هَرَبًا ﴿١٢﴾ وَأَنَّا لَمَّا سَمِعْنَا الْهُدَىٰ
آمَنَّا بِهِ ۖ فَمَن يُؤْمِن بِرَبِّهِ فَلَا يَخَافُ بَخْسًا وَلَا رَهَقًا ﴿١٣﴾

(2) Ikuitanira ku chilungamo, ndipo taikhulupirira. Sitim'phatikiza aliyense ndi Mbuye wathu (pa mapemphero).

1-2 Nena (iwe Mtumiki (SAW) kuti: "Allah wavumbulutsa kwa ine kuti ndithu gulu lina la ziwanda lidamvetsera kuwerenga kwanga kwa Qur'aan. Pamene adaimva adanena kwa anthu awo kuti: ndithu ife taimva Qur'aan yozama kwambiri pa kufikitsa matanthauzo ake, mvemvemve wake, nzeru zake, malamulo ake ndi nkhani zake. Ikuitanira ku choonadi ndi chiongoko tero ife taivomereza Qur'aan imeneyi ndipo taigwiritsira ntchito, ndipo sitidzam'phatikizanso Mbuye wathu Amene adatilenga ndi wina aliyense pomupembedza.]

(3) "Ndipo ndithu, ukulu ndi ulemerero wa Mbuye wathu watukuka; sadadzipangire mkazi kapena mwana. [Ndipo ndithu watukuka ukulu ndi ulemerero wa Mbuye wathu, sadadziikire Yekha mkazi kapena mwana].

(4) "Ndipo ndithu , mbuli za mwa ife zakhala zikunenera Allah mawu abodza (okhala kutali ndi choonadi). [Ndipo ndithu, mbuli yathu amene ali Iblis (kholo la asatana) adali kumunenera Allah Taalaa liwu lotalikira ku choonadi pomunamizira kuti ali ndi mkazi ndi mwana].

(5) "Ndipo ndithu ife tinkaganiza kuti anthu ndi ziwanda sangam'nenere Allah zabodza (zosayenera ulemerero Wake).

[Ndikutinso ife tinkaganiza kuti palibe wina aliyense angam'namizire Allah Taalaa, osakhala mwa anthu ngakhalenso mu ziwanda pomuchitira Allah kuti ali ndi mkazi ndi mwana].

(6) "Ndithu, padali amuna a muwanthu amapempha chitetezo kwa amuna a m'ziwanda, ndipo adawaonjezera (amuna a m'ziwanda) kupitiriza machimo awo, kupulukira (ndi kuchenjerera anthu).

[Ndipo ndithu adali amuna ena a mwa anthu akumapempha chipulumutso ndi amuna ena a mu ziwanda kotero amuna a m'ziwanda adawawonjezera amuna a mu anthuwo pakupempha kwawo chitchinjirizo kwa iwo, chiopsezo ndi mantha. Kupempha chitchinjirizo ndi zina zake zosakhala Allah zomwe Allah adawadetsera nazo anthu a umbuli, zili m'gulu la shirk yaikulu yomwe Allah sangaikhululukire pokhapokha ndi kulapa kwenikweni kwa Iye. Ndipo mu Ayah imeneyi, muli chenjezo lalikulu loletsa kupempha chitchinjirizo chilichonse kwa afiti, amatsenga ndi ofanana ndi iwo.]

(7) "Ndipo iwo amaganiza monga momwe mumaganizira inu kuti Allah sadzaukitsa aliyense (atafa). [Ndikutinso ndithu makafiri a muwanthu amaganiza monga m'mene mumaganizira inu ziwanda kuti ndithu Allah Taalaa sadzaukitsa wina aliyense pambuyo pa imfa.]

(8) "Ndithu, ife tidafuna kukafika kumwamba; tidakupeza kutadzala alonda (angero) amphamvu ndi zenje za moto. [Ndipo ndithu ife gulu la ziwanda tidzafuna kukafika ku thambo kukamvera mawu a eni thambolo, ndiye tidalipeza litadzadzidwa ndi angero ambiri amene akulilondera komanso zenje zowotcha zimene akugendedwa nazo amene akuliyandikira].

(9) "Ndithu ife tidali kukhala m'menemo (kale) mokhala momvetsera; (mobera nkhani za kumwamba). Koma amene afune kumvetsera tsopano, apeza chenje cha moto chikudikirira (kuti chim'gwere iye ndi kumuononga).[Ndithu ife tidali isadafike nyengo imeneyi tikudzichitira ku thambo malo kuti tidzikamvetsera nkhani za m'menemo. Ndipo amene ayesere tsopano kukabera kumvetsera, amakapeza kwa iye chenje chili tcheru, chimamuotcha ndi kumuononga. Mu ma Ayah awiri amenewa muli umboni wotsutsa kudzikundikira kwa afiti ndi a matsenga amene amadzinamiza kuzindikira

zinthu zobisika nkumanyenga anthu a nzeru zofooka ndi bodza lawolo ndi kupekerako.]

(10) “Ndithu, ife sitikudziwa chilango chimene akuwafunira a m’dziko (polonda kumwamba kuletsa kumvetsera nkhani za kumeneko); kapena Mbuye wawo akuwafunira zabwino ndi chilungamo (pa zimenezo).

[Ndthudi ife a gulu la ziwanda sitikudziwa kuti kodi n’zoipa zimene Allah wafuna kuti awatsitsire anthu a pa dziko lapansi kapena wafunira zabwino ndi chiongoko?]

(11) “Ndithu, ena mwa ife ndi abwino koma ena sali choncho; tili njira zosiyanasiyana.

[Ndipo ndithu mwa ife muli ena abwino, oopa komanso ena mwa ife amene sali dero, makafiri ndi owononga, tili magulumagulu ndi njira zosiyanasiyana.]

(12) “Ndithu ife, tidadziwa kuti Allah sitingathe kum’lepheretsa (lamulo Lake pa ife paliponse tingakhale) pa dziko lapansi, ndipo sitingam’lepheretsenso pom’zemba ndi kuthawira (kumwamba) [Ndithudi ife tatsimikiza kuti ndithu Allah ndi Wakuthekera pa ife ndikuti ifeyo tili m’dzanja Mwake ndi mu ufumu Wake, ndipo sitidzatha kumuzemba Iye akatifunira kutichita kanthu kalikonse, ndipo sitidzatha kupulumuka ku chilango Chake pothawira kumwamba ngati atatifunira zoipa].

(13) “Ndipo ife pamene tachimva chiongoko (Qur’aan) tachikhulupirira ndipo amene ati akhulupirire mwa Mbuye wake saopa kum’chepetsera (chabwino kapena kumuonjezera machimo ake). [Ndithu ife pamene taimva Qur’aan, taikhulupirira ndipo tavomereza zoti imeneyi ndi yoona yochokera kwa Allah. Kotero amene angakhulupirire Mbuye ndithu iye saopa kupungulidwa mu zabwino zake kapena kupondereza.

kumene kungam’peze powonjezera zoipa zake].

(14) “Ndithu mwa ife alipo Asilamu ndipo mwa ife alipo opatuka mu njira ya chilungamo; amene walowa m’Chisilamu, iwowo ndi amene akulunjika mu njira ya choonadi.

(15) “Koma opatuka (ku chiongoko) adzakhala nkhuni za jahena.”

14-15 [Ndithudi ena mwa ife alipo amene amadzichepetsa kwa Allah pomumvera ndipo mwa ife muli ena amene ali opyola malire, opondereza amene apotoka kusiya njira ya choonadi. Ndipo amene akhale Msilamu ndi kudzichepetsa kwa Allah pomvera, iwowo ndi omwe alunjika njira yachoonadi ndi yolondola ndiponso wachitira khama pakusankha kwake kotero Allah wawawongolera ku njira

وَأَنَّا مِنَّا ٱلْمُسْلِمُونَ وَمِنَّا ٱلْقَٰسِطُونَ فَمَنْ أَسْلَمَ فَأُوْلَٰٓئِكَ
تَحَرَّوْاْ رَشَدًا ﴿١٤﴾ وَأَمَّا ٱلْقَٰسِطُونَ فَكَانُواْ لِجَهَنَّمَ حَطَبًا ﴿١٥﴾
وَأَلَّوِ ٱسْتَقَٰمُواْ عَلَى ٱلطَّرِيقَةِ لَأَسْقَيْنَٰهُم مَّآءً غَدَقًا ﴿١٦﴾ لِّنَفْتِنَهُمْ
فِيهِ ۚ وَمَن يُعْرِضْ عَن ذِكْرِ رَبِّهِۦ يَسْلُكْهُ عَذَابًا صَعَدًا ﴿١٧﴾ وَأَنَّ
ٱلْمَسَٰجِدَ لِلَّهِ فَلَا تَدْعُواْ مَعَ ٱللَّهِ أَحَدًا ﴿١٨﴾ وَأَنَّهُۥ لَمَّا قَامَ عَبْدُ ٱللَّهِ
يَدْعُوهُ كَادُواْ يَكُونُونَ عَلَيْهِ لِبَدًا ﴿١٩﴾ قُلْ إِنَّمَآ أَدْعُواْ رَبِّى وَلَآ أُشْرِكُ
بِهِۦٓ أَحَدًا ﴿٢٠﴾ قُلْ إِنِّى لَآ أَمْلِكُ لَكُمْ ضَرًّا وَلَا رَشَدًا ﴿٢١﴾ قُلْ إِنِّى
لَن يُجِيرَنِى مِنَ ٱللَّهِ أَحَدٌ وَلَنْ أَجِدَ مِن دُونِهِۦ مُلْتَحَدًا ﴿٢٢﴾ إِلَّا بَلَٰغًا
مِّنَ ٱللَّهِ وَرِسَٰلَٰتِهِۦ ۚ وَمَن يَعْصِ ٱللَّهَ وَرَسُولَهُۥ فَإِنَّ لَهُۥ نَارَ جَهَنَّمَ
خَٰلِدِينَ فِيهَآ أَبَدًا ﴿٢٣﴾ حَتَّىٰٓ إِذَا رَأَوْاْ مَا يُوعَدُونَ فَسَيَعْلَمُونَ
مَنْ أَضْعَفُ نَاصِرًا وَأَقَلُّ عَدَدًا ﴿٢٤﴾ قُلْ إِنْ أَدْرِىٓ أَقَرِيبٌ
مَّا تُوعَدُونَ أَمْ يَجْعَلُ لَهُۥ رَبِّىٓ أَمَدًا ﴿٢٥﴾ عَٰلِمُ ٱلْغَيْبِ فَلَا
يُظْهِرُ عَلَىٰ غَيْبِهِۦٓ أَحَدًا ﴿٢٦﴾ إِلَّا مَنِ ٱرْتَضَىٰ مِن رَّسُولٍ فَإِنَّهُۥ
يَسْلُكُ مِنۢ بَيْنِ يَدَيْهِ وَمِنْ خَلْفِهِۦ رَصَدًا ﴿٢٧﴾ لِّيَعْلَمَ أَن قَدْ أَبْلَغُواْ
رِسَٰلَٰتِ رَبِّهِمْ وَأَحَاطَ بِمَا لَدَيْهِمْ وَأَحْصَىٰ كُلَّ شَىْءٍ عَدَدًا ﴿٢٨﴾

imeneyo. Tsono amene akupyola malire ndi kusiya njira ya Chisilamu, ndiye kuti ali nkhuni za ku jahena.]

(16) Ndithu, (anthu ndi ziwanda) akadalungama pa njira (ya chilungamo), tikadawamwetsa madzi ambiri (okwanira nyengo zonse).

(17) Kuti tiwayese ndi zimenezo (m’mene angamuyamikire Allah pa mtendere Wake pa iwo). Koma amene anyozera kupembedza Mbuye wake, am’lowetsa ku chilango chovuta (chimene sangathe kupirira nacho).

16-17 [Ndithudi, adakayenda makafiri a mu wanthu komanso a mu ziwanda pa njira ya Chisilamu, napanda kupotoka kuisiya njirayo, bwenzi titawatumizira madzi ambiri komanso bwenzi titawachulukitsira riziq pa dziko lapansi kuti tiwayese mayeso m’mene angayamikire mtendere wa Allah umene uli pa iwo. Amene atembenuke kusiya kumvera Mbuye wake ndi kuimvetsera Qur’aan komanso kuiganizira ndi kuigwiritsira ntchito, akamulowetsa mu chilango chowawitsa].

(18) Ndithu, misikiti ndi ya Allah Yekha, kotero musapembedze aliyense pamodzi ndi Allah.

[Ndipo ndithu misikiti ndi yopempbedzera

Allah Yekha choncho musapembedze m'menemo wina aliyense wosakhala Allah. Ndipo dziyeretseni kwa Iye pochita du'aa ndi ibaadah m'menemo. Popeza misikiti siinamangidwe kupatula ndi cholinga choti adzipembedzedwa Allah Yekha m'menemo osati wina aliyense wosakhala Iye. M'menemu muli chikakamizo choyeretsa misikiti ku china chilichonse chodetsa kudziyeretsera kwa Allah ndi kutsatira Mtumiki Wake Muhammad (SAW)].

(19) Ndipo ndithu, pamene adaima kapolo wa Allah (Muhammad (SAW) pa swalaat yake)uku akum'pembedza Iye (Allah), ziwanda zidatsala pang'ono kumugwera (chifukwa cha kuchuluka kwawo ndi kum'zinga podabwa ndi zimene adaziona ndi kuzimva). [Ndithudi pamene adaima Muhammad (SAW) akupembedza Mbuye wake, zidayandikira ziwanda kugwera iye zili magulumagulu zina pamwamba pa zina chifukwa chochuluka chipwirikiti chawo pomvetsera Qur'aan kwa iye (SAW).

(20) Nena: "Ndikum'pembedza Mbuye wanga Mmodzi (Yekha) ndipo sindingam'phatikize ndi aliyense m'mapemphero Ake)".

[Nena iwe Mtumiki (SAW) kwa makafiri amenewa kuti: "Ndithudi ine ndikupembedza Mbuye wanga Yekhayo ndipo sindingam'phatikize limodzi Naye popembedzapo wina aliyense].

(21) Nena: "Ine ndilibe udindo wokupatsani mavuto kapena chilungamo (ndi zabwino)".

(22) Nena: "Ine palibe anganditeteze ku chilango cha Allah (ngati nditam'nyoza) sindingapeze malo wothawira ku chilango Chake kupatula kwa Iye."

(23) "Koma mphamvu imene ndili nayo ndi kufikitsa uthenga wa Allah umene adanditumizira . ndithu amene anyoze Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) (ndi kupatuka pa chipembedzo cha Allah) ndithu moto wa jahena ndi wake akakhala m'menemo muyaya."

21-23 [Nena iwe Mtumiki (SAW) kwa iwo kuti ndithudi ine sindingathe kukutchinjirizani inu ku choipa kapena kukubweretserani thandizo. Nena: ndithu ine palibe amene adzandipulumutse ku chilango cha Allah ngati nditam'nyoza ndipo sindidzapeza kopanda kwa Iye kodalira , kuti ndithawireko ku chilango cha Allah. Koma zimene zili m'manja mwanga ndi zokufikitsirani inu zimene wandilamula Allah kufikitsa kwa inu, ndi uthenga Wake umene wanditúma nawo kwa inu. Amene anyoze Allah ndi Mtumiki Wake (SAW), nataya chipembedzo cha Allah, ndithu malipiro ake ndi moto wa jahena womwe sakatulukamo mpaka muyaya.]

(24) Mpaka pomwe adzaziona zimene alonjezedwa ndi pamene adzadziwa (kuti) kodi ndani mwini mthandizi wofooka ndiponso wochepekedwa kuchuluka (kwa om'tsatira, iwo kapena Asilamu). [Kufikira pamene anthu opembedza mafano adzaone zomwe akulonjezedwazo za chilango, ndipamene adzazindikire pa nthawi yowapeza chilangocho kuti ndi uti amene ali mthandizi wofooka komanso wochepekera kuchuluka kwa asilikali ake].

(25) Nena kuti: "Sindikudziwa ngati zomwe mukulonjezedwa (za chilango) zili pafupi kapena Mbuye wanga wazitalikitsa,

(26) "Iye ndi Wodziwa zobisika, sazionetsa zobisika Zake kwa aliyense (m'zolengedwa Zake),

(27) "Kupatula Mtumiki (wake) amene wamuyanja (iyeyo amam'dziwitsa zobisikazo) ndipo ndithu amamuikira omulonda omayenda kutsogolo kwake ndi kumbuyo kwake,

(28) "Kuti adziwe ngati afikitsa uthenga wa Mbuye wawo, ndipo wawazungulira (podziwa zonse zili kwa iwo) ndipo wadziwa kuchuluka kwa zinthu zonse zimene zilipo (palibe chobisika kwa Iye)".

25-28 [Nena iwe Mtumiki (SAW) kwa mamushrikina amenewa kuti: "Sindikudziwa kodi chilango chimene inu mwalonjezedwa nacho nthawi yake yayandikira kapena Mbuye wanga aichita kukhala yotalikira? Iye Subhaanahu ndi Wodziwa zimene zabisika ku maso (a zolengedwa) kotero saonetsa zobisika Zakezo kwa aliyense mu zolengedwa Zake kupatula amene wamusankha kum'patsa utumiki Wake ndi kumuyanja, ndiye Iye amaonetsera amenewa zina mwa zobisika Zake; ndipo amatumiza patsogolo pa Mtumikiyo ndi kumbuyo kwake angero amene amamuteteza ku ziwanda kuti asamunong'onezere ndi kumusokoneza kwa alosi. Zimenezi kuti azindikire Mtumiki (SAW) kuti atumiki amene anadza iye asanadze adali m'mene alili iyeyu (SAW) pa zakafikitsidwe ka choonadi ndi kuona mtima ndikutinso iyeyu (SAW) watetezedwa monga m'mene Atumikiwo anatetezedwera ku ziwanda. Komanso ndikuti ndithu Allah Subhaanahu kuzindikira Kwake kwazizinga zimenezo (zolengedwa) zili nazo zoonekera kapena zobisika mu malamulo ndi kakonzedwe ka zinthu mwa luntha ndi zina zotero. Palibe chinthu chilichonse chimene chimamudutsa ndikutinso ndithudi Iye Wapamwambamwamba waziwerenga zinthu zonse kuchuluka kwake kotero palibe chinthu chimene chabisika kwa Iye.]

# (73) SUURAT MUZ'ZAM'MIL

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Ee, iwe wadziphimba (ndi nsalu)!

2 Imirira usiku (upemphere) kupatula nthawi yochepa.

3 Theka lake kapena chepetsa thekalo pang'ono (mpaka ufike chimodzi mwa zigawo zitatu za usiku).

4 Kapena wonjezerapo (mpaka ufike zigawo ziwiri mwa zigawo zitatu za usiku) ndipo werenga Qur'aan mofatsa (lemba ndi lemba).

[Ee, iwe amene wadziphimba ndi nsalu zake! Imirira kupemphera mu usiku kupatula nyengo yochepa ya usikuwo. Imirira theka la usiku kapena punguza mu thekalo pang'ono kufikira gawo limodzi mwa zigawo zitatu za usikuwo kapena wonjezera pa thekalo kufikira kufika pa zigawo ziwiri mwa zigawo zitatu za usiku. Ndipo werenga Qur'aan modekha, motsindika lemba ndi lemba komanso mopumira mwake].

5 Ndithu Ife tikuvumbulutsira iwe (Mneneri SAW) mawu olemera (omwe ndi Qur'aan).

[Ndithu Ife tikukutumizira iwe Mneneri (SAW) Qur'aan yaikulu imene m'kati mwake mukhalemo zolamulidwa, zoletsedwa ndi malamulo a Shariah].

6 Ndithu kudzuka kwa usiku ndi kuchita mapemphero kumalowerera (mu mtima) kwambiri, ndipo zoyankhula zake zimakhala zoongoka ndi zolunjika bwino (kuposa mapemphero a masana).

[Ndithu mapemphero amene amapangidwa mkati mwa usiku ndi amene amakhudza mtima kwambiri komanso limakhala liwu lomveka bwino chifukwa choti mtima umakhala usakutanganidwa ndi ntchito za pa dziko lapansi (zomwe zimagwirika masana)].

7 Ndithu, masana uli ndi zochitikachitika zambiri (umatanganidwa ndi ntchito ya uthenga, dzipatse danga usiku polimbika kupemphera).

[Ndithu masana uli nako kutanganidwa ndi kutembenukatembenuka ku zinthu zokukomera ndi ntchito zochuluka zokhudzana ndi utumiki, choncho dzipatse nthawi usiku yomupempherera Mbuye wako.]

8 Tchula dzina la Mbuye wako (Amene adalenga ndi kulera zinthu) ndipo udzipereke kwathunthu kwa Iye.

9 (Iye ndiye) Mbuye wa kuvuma ndi kuzambwe; palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma Iye; m'chiteni kukhala mtetezi (wanu pa zinthu zanu zonse).

8-9 [Tchula iwe Mneneri (SAW) dzina la Mbuye wako, choncho m'pemphe kudzera mu dzina limenelo ndipo kwa Iye dzipereke kwathunthu pa mapemphero ako komanso

سُورَةُ المُزَّمِّل
ترتيبها ٧٣
آياتها ٢٠

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

يَٰٓأَيُّهَا ٱلۡمُزَّمِّلُ ١ قُمِ ٱلَّيۡلَ إِلَّا قَلِيلٗا ٢ نِّصۡفَهُۥٓ أَوِ ٱنقُصۡ مِنۡهُ قَلِيلًا
٣ أَوۡ زِدۡ عَلَيۡهِ وَرَتِّلِ ٱلۡقُرۡءَانَ تَرۡتِيلًا ٤ إِنَّا سَنُلۡقِي عَلَيۡكَ قَوۡلٗا
ثَقِيلًا ٥ إِنَّ نَاشِئَةَ ٱلَّيۡلِ هِيَ أَشَدُّ وَطۡـٔٗا وَأَقۡوَمُ قِيلًا ٦ إِنَّ لَكَ فِي
ٱلنَّهَارِ سَبۡحٗا طَوِيلٗا ٧ وَٱذۡكُرِ ٱسۡمَ رَبِّكَ وَتَبَتَّلۡ إِلَيۡهِ تَبۡتِيلٗا ٨
رَّبُّ ٱلۡمَشۡرِقِ وَٱلۡمَغۡرِبِ لَآ إِلَٰهَ إِلَّا هُوَ فَٱتَّخِذۡهُ وَكِيلٗا ٩ وَٱصۡبِرۡ
عَلَىٰ مَا يَقُولُونَ وَٱهۡجُرۡهُمۡ هَجۡرٗا جَمِيلٗا ١٠ وَذَرۡنِي وَٱلۡمُكَذِّبِينَ
أُوْلِي ٱلنَّعۡمَةِ وَمَهِّلۡهُمۡ قَلِيلًا ١١ إِنَّ لَدَيۡنَآ أَنكَالٗا وَجَحِيمٗا ١٢
وَطَعَامٗا ذَا غُصَّةٖ وَعَذَابًا أَلِيمٗا ١٣ يَوۡمَ تَرۡجُفُ ٱلۡأَرۡضُ وَٱلۡجِبَالُ
وَكَانَتِ ٱلۡجِبَالُ كَثِيبٗا مَّهِيلًا ١٤ إِنَّآ أَرۡسَلۡنَآ إِلَيۡكُمۡ رَسُولٗا شَٰهِدًا
عَلَيۡكُمۡ كَمَآ أَرۡسَلۡنَآ إِلَىٰ فِرۡعَوۡنَ رَسُولٗا ١٥ فَعَصَىٰ فِرۡعَوۡنُ ٱلرَّسُولَ
فَأَخَذۡنَٰهُ أَخۡذٗا وَبِيلٗا ١٦ فَكَيۡفَ تَتَّقُونَ إِن كَفَرۡتُمۡ يَوۡمٗا يَجۡعَلُ
ٱلۡوِلۡدَٰنَ شِيبًا ١٧ ٱلسَّمَآءُ مُنفَطِرُۢ بِهِۦۚ كَانَ وَعۡدُهُۥ مَفۡعُولًا ١٨
إِنَّ هَٰذِهِۦ تَذۡكِرَةٞۖ فَمَن شَآءَ ٱتَّخَذَ إِلَىٰ رَبِّهِۦ سَبِيلًا ١٩

yedzamira pa Iye, Iye ndi Mwini kuvuma ndi kuzambwe palibe wopembedzedwa wina mwa choonadi kupatula Iye, kotero tsamira pa Iye komanso zinthu zako zonse zipereke kwa Iye.]

10 Ndipo pirira (pa zabodza) zimene akunena. Apewe (ndi mtima wako) kupewa kwabwino.

[Pirira pa zomwe akuziyankhula mamushrikina zokhudza iwe ndi chipembedzo chako, ndipo semphana nawo mu zochita zawo zabodza pamodzi ndi kuwatalikira iwowo ndi kusiya kubwezera choipa].

11 Ndisiye Ine ndi otsutsawa, eni kupeza bwino ndipo alekerere kanthawi kochepa.

[Ndisiye iwe Mtumiki (SAW) ndi okanirawa ma Ayah Anga, anamadya bwino pa dziko lapansi, ndipo alekerere kanthawi kochepa powachedwetsera chilango kwa iwo kufikira idzakwane nyengo imene idalembedwa yowalangira iwo].

12 Ndithudi tili ndi mitundumitundu ya unyolo ndi moto woyaka,

13 Ndi chakudya chotsamwitsa ndi chilango chowawitsa.

12-13 [Ndithu iwowa ali nawo kwa Ife maunyolo olemera komanso moto woyaka ndipo umenewo akaotchedwa nawo, komanso chakudya choipa

chotsamwitsa pa khosi komanso chosadzetsa mudyo ndi chilango chopweteka zedi].

14 Tsiku limene nthaka ndi mapiri zidzagwedezeka (kugwedezeka kwa mphamvu kotero kuti) mapiri adzakhala ngati mulu wa mchenga woyoyoka.[Tsiku limene nthaka ndi mapiri adzatekeseke kufikira kuti mapiri adzakhala ngati mulu wa mchenga womauluzika nkuyoyoka pambuyo poti udali wolimba,wouma].

15 Ndithu, Ife takutumizirani Mtumiki (SAW) amene adzakhala mboni yanu (Tsiku Lomaliza) monga momwe tidam'tumizira (Mussa (AS) kukhala) Mtumiki kwa Farawo.

16 Koma Farawo adam'nyoza Mtumikiyo ndipo tidamulanga chilango chokhwima.

15-16 [Ndithu Ife tatumiza kwa inu anthu a pa Makka Muhammad (SAW) kukhala Mtumiki wochitira umboni pa inu mu zomwe zatuluka kuchokera kwa inu mu ukafiri ndi kunyoza, monga m'mene tidamutumizira Musa (AS) kukhala Mtumiki kwa Farawo – munthu wopyola malire- koma Farawo adam'kanira Mussa (AS) ndipo sadakhulupirire za utumiki wake komanso adanyoza lamulo lake, ndiye tidamuononga kumuononga kolapitsa. M'menemu muli chenjezo loti anthu asamanyoze Mtumiki Muhammad (SAW) kuopa kuti wonyozayo zingam'peze zofanana ndi zimene zidam'peza Farawo ndi anthu ake.]

17 Kodi mungadzitchinjirize chotani ngati mukana (chilango cha) tsiku (lomwe) lidzachititsa ana kukhala ndi imvi? [Nanga motani mudzatha kudzitchinjiriza nokha –ngati mutakanira – ku chilango cha Tsiku Lakiyama limene lidzachititse ana ang'ono kukhala ndi imvi chifukwa cha zoopsa ndi mavuto ake.]

18 Thambo (pamodzi ndi mphamvu zake ndi kukula kwake), lidzang'ambika (tsiku limenelo) chifukwa cha kuopsa kwa tsikulo; lonjezo la Allah lidzakwaniritsidwa (palibe wolipinga).

[Thambo lidzang'ambikang'ambika pa tsiku limenelo chifukwa cha kuopsa kwake kwakukulu. Lonjezo la Allah Taalaa lobwera tsiku limeneli lili lochitika basi popanda chikaiko].

19 Ndithudi, ma Ayah awa (amene akunena za kuopsa kwa Kiyama) ndi chikumbutso, choncho amene akufuna (kuthandizika nawo) ayende pa njira ya Mbuye wake (pokwaniritsa malamulo Ake ndi kuleka zoipa)

[Ndithu ma Ayah oopsawa omwe mkati mwake muli zoopsa ndi kukalipa ndi ulaliki komanso lingaliro kwa anthu. Amene akufuna kupezamo malingaliro ndi kuthandizika nawo, akuchita kumvera ndi kuopa kukhala njira imene ingamufikitse ku chiyanjo cha Mbuye wake Amene adamulenga ndi kumulera].

20 Ndithu, Mbuye wako akudziwa kuti iwe ukuima (kupemphera) pafupifupi zigawo ziwiri mwa zigawo zitatu za usiku kapena theka lake, kapenanso chigawo chimodzi mwa zigawo zitatu za usiku, pamodzi ndi anthu ena omwe uli nawo (naonso akuchita chimodzimodzi). Allah ndi Amene amadziwa bwino muyeso wa (nthawi za) usiku ndi usana. Wadziwa kuti simungathe kuwerenga zimenezo, choncho wakukhululukirani. Werengani ndime imene yapepuka yochokera m'Qur'aan. Wadziwa kuti ena mwa inu adzakhala odwala (kudzawavuta kuimirira ndi kuchezera usiku) ndipo ena adzakhala akuyendayenda pa dziko (ndi cholinga cha malonda ndi ntchito) kunka nafunafuna ubwino wa Allah. Ndipo ena adzakhala akumenya nkhondo pa njira ya Allah (n'cholinga chotukula mawu Ake), werengani chimene chapepuka chochokera m'menemo (m'Qur'aan) ndipo pitirizani kupemphera swalaat, perekani chopereka (chimene chakakamizidwa kwa inu). Ndipo mkongozeni Allah ngongole yabwino, ndipo chilichonse chabwino chimene mwadzitsogozera, mudzachipeza kwa Allah chili chabwino ndi malipiro akulu zedi. Ndipo m'pempheni Allah chikhululuko. Ndithu Allah Ngokhululuka, Ngwachisoni.

[Ndithu Mbuye wako iwe Mneneri (SAW) akudziwa kuti ndithu iwe ukuimirira kupemphera tahajjud (usiku) mu gawo la usiku lochepera zigawo zake ziwiri nthawi zina ndipo umaimirira kupemphera theka lake nthawi zina. Umaimiriranso kupemphera gawo limodzi mwa zigawo zitatu za usiku nthawi zina ndipo limaimirira kupemphera nawe gulu la maswahaba ako. Allah Yekhayo ndi Amene amalinganiza (kutalika kwa nyengo za) usiku ndi usana komanso amazindikira miyezo ya ziwirizi ndi zimene zikudutsa ndi zomwe zikutsala. Allah wadziwa kuti padzapezeka mwa inu amene matenda adzamulepheretse kuima kupemphera usiku. Ndipo adzapezeka anthu ena akuyendayenda pa dziko kokachita malonda ndi ntchito ndi kufunafuna riziq la Allah la halaal. Ndipo anthu ena adzakhala akuchita jihad mu njira ya Allah pofuna kutukula liwu Lake ndi kufalitsa chipembedzo Chake. Choncho bawerengani mu swalaat zanu zomwe zakupepukirani za m'Qur'aan, ndipo dzizolowezeni kupemphera mapemphero asanu achikakamizo ndipo perekani zakaat yachikakamizo kwa inu ndipo mudziperekanso sadaka mu njira ya zabwino ndi kuchitira zabwino ena kuchokera mu chuma chanu

pofunafuna nkhope ya Allah. Ndipo kalikonse mu mitundu ya zabwino, zokomera anthu ndi ntchito zomvera, mukapeza nazo malipiro ndi mphoto zake kwa Allah Tsiku Lakiyama zili zabwino kuposa m'mene mudazitsogozera pa dziko lapansi komanso zili ndi malipiro oposa m'mene zidalili. Ndipo funafunani chikhululuko cha Allah mu kukhala kwanu konse, ndithu Allah ndi Wokhululuka kwambiri kwa inu komanso Wachisoni ndi inu.]

## (74) SUURAT –UL-MUD'DATH'IR

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Ee, iwe wadziphimba nsalu!

(2) Imirira ndipo uchenjeze (anthu za chilango cha Allah akapanda kukhulupirira).

(3) Ndipo Mbuye wako (Yekha) um'kulitse (pomulemekeza.

(4) Ndipo nsalu zako uziyeretse (ndi madzi ku uye).

(5) Ndiponso zoipa (mafano) zipewe.

(6) Usapatse (anthu) n'cholinga choti ulandire zambiri.

(7) Chifukwa cha Mbuye wako, pirira (ku malamulo Ake poleka zomwe waletsa ndi kuchita zimene walamula).

1-7 [Ee, iwe amene wadziphimba ndi nsalu zake, imirira kusiya malo ako ogona ndipo uchenjeze anthu za chilango cha Allah. Lunjika Mbuye wako Yekha ndi kumukuza ndi umodzi Wake komanso pomupembedza. Ndipo zovala zako uziyeretse ku zonyansa popeza kudziyeretsa kwa kunja (koonekera) kuli mu gulu lokwaniritsa kuyera kwamkati. Ndipo upitirire posamukira mafano , milungu yabodza ndi ntchito zonse za shirk, usaziyandikire. Ndiponso usapereke chopereka ndi chifukwa choti upeze zochuluka kuposa izo. Ndiponso chifukwa chosangalatsa Mbuye wako pirira pa zolamulidwa ndi zoletsedwa.

(8) Likadzaimbidwa lipenga,

(9) Tsiku limenelo lidzakhala tsiku lovuta.

(10) Kwa osakhulupirira, silidzakhala lofewa.

8-10 [Likadzauziridwa lipenga kuuzira kodzutsa zolengedwa kwa akufuna ndi kusonkhanitsidwa (ku bwalo la chiweluzo), ndiyetu nthawi imeneyo ndi tsiku lovuta kwambiri kwa osakhulupirira, sikuti kwa iwo ndi lophweka kufikira koti amalize mu zomwe iwo alili zofunsidwa kuwerengeredwa ntchito zawo ndi zina zotero mu zinthu zoopsa.]

(11) Ndisiye ndi amene ndidam'lenga Ndekha,

(12) Ndipo ndam'patsa chuma chamberi.

(13) Ndi ana omwe amakhala nawo (paliponse).

۞ إِنَّ رَبَّكَ يَعْلَمُ أَنَّكَ تَقُومُ أَدْنَىٰ مِن ثُلُثَيِ ٱلَّيْلِ وَنِصْفَهُۥ وَثُلُثَهُۥ وَطَآئِفَةٌ
مِّنَ ٱلَّذِينَ مَعَكَ ۚ وَٱللَّهُ يُقَدِّرُ ٱلَّيْلَ وَٱلنَّهَارَ ۚ عَلِمَ أَن لَّن تُحْصُوهُ فَتَابَ
عَلَيْكُمْ ۖ فَٱقْرَءُوا۟ مَا تَيَسَّرَ مِنَ ٱلْقُرْءَانِ ۚ عَلِمَ أَن سَيَكُونُ مِنكُم مَّرْضَىٰ ۙ
وَءَاخَرُونَ يَضْرِبُونَ فِى ٱلْأَرْضِ يَبْتَغُونَ مِن فَضْلِ ٱللَّهِ ۙ وَءَاخَرُونَ
يُقَٰتِلُونَ فِى سَبِيلِ ٱللَّهِ ۖ فَٱقْرَءُوا۟ مَا تَيَسَّرَ مِنْهُ ۚ وَأَقِيمُوا۟ ٱلصَّلَوٰةَ وَءَاتُوا۟
ٱلزَّكَوٰةَ وَأَقْرِضُوا۟ ٱللَّهَ قَرْضًا حَسَنًا ۚ وَمَا تُقَدِّمُوا۟ لِأَنفُسِكُم مِّنْ خَيْرٍ تَجِدُوهُ
عِندَ ٱللَّهِ هُوَ خَيْرًا وَأَعْظَمَ أَجْرًا ۚ وَٱسْتَغْفِرُوا۟ ٱللَّهَ ۖ إِنَّ ٱللَّهَ غَفُورٌ رَّحِيمٌۢ ﴿٢٠﴾

### سُورَةُ المُدَّثِّر

ترتيبها ٧٤ — آياتها ٢٠

بِسْمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحْمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

يَٰٓأَيُّهَا ٱلْمُدَّثِّرُ ﴿١﴾ قُمْ فَأَنذِرْ ﴿٢﴾ وَرَبَّكَ فَكَبِّرْ ﴿٣﴾ وَثِيَابَكَ فَطَهِّرْ ﴿٤﴾
وَٱلرُّجْزَ فَٱهْجُرْ ﴿٥﴾ وَلَا تَمْنُن تَسْتَكْثِرُ ﴿٦﴾ وَلِرَبِّكَ فَٱصْبِرْ ﴿٧﴾
فَإِذَا نُقِرَ فِى ٱلنَّاقُورِ ﴿٨﴾ فَذَٰلِكَ يَوْمَئِذٍ يَوْمٌ عَسِيرٌ ﴿٩﴾ عَلَى ٱلْكَٰفِرِينَ
غَيْرُ يَسِيرٍ ﴿١٠﴾ ذَرْنِى وَمَنْ خَلَقْتُ وَحِيدًا ﴿١١﴾ وَجَعَلْتُ لَهُۥ مَالًا
مَّمْدُودًا ﴿١٢﴾ وَبَنِينَ شُهُودًا ﴿١٣﴾ وَمَهَّدتُّ لَهُۥ تَمْهِيدًا ﴿١٤﴾ ثُمَّ يَطْمَعُ
أَنْ أَزِيدَ ﴿١٥﴾ كَلَّآ ۖ إِنَّهُۥ كَانَ لِءَايَٰتِنَا عَنِيدًا ﴿١٦﴾ سَأُرْهِقُهُۥ صَعُودًا ﴿١٧﴾

(14) Ndipo ndam'konzera (ulemerero) kum'konzera (kwabwino).

(15) Kenako ali ndi dyera kuti ndimuonjezere (zina popanda kuthokoza).

(16) Koma sichoncho! Ndithu, iye adali kutsutsa zizindikiro Zathu.

(17) Ndidzam'kakamiza ku chilango chovuta (kukwera phiri la ku moto limene sakatha kulikwera).

11-17 [Ndisiye Ine iwe Mtumiki (SAW) ndi amene ndidamulenga m'mimba mwa mayi wake ali yekhayekha wopanda chuma ngakhalenso mwana, ndipo ndamupatsa chuma chotambasuka chambirimbiri komanso ana okhala nawo pomwepo nthawi zonse mu mzinda wa Makka omwe sasowa kwa iye. Ndipo ndamufewetsereratu njira zopezera zosoweka za moyo. Kenaka ati akulakalaka pambuyo pomupatsa zonsezi kuti ndimuonjezere mu chuma chake komanso ana ake kumachita iye adakanira Ine. Zinthu sizili monga akuganizira munthu woipitsayu, wamachimo. Ine sindimuonjezera pa zimenezo . Iye pa Qur'aan ndi zitsimikiziro za Allah kwa zolengedwa Zake adali wamankhalu, wokanira. Ndidzam'panikiza

إِنَّهُۥ فَكَّرَ وَقَدَّرَ ﴿١٨﴾ فَقُتِلَ كَيْفَ قَدَّرَ ﴿١٩﴾ ثُمَّ قُتِلَ كَيْفَ قَدَّرَ ﴿٢٠﴾ ثُمَّ نَظَرَ
﴿٢١﴾ ثُمَّ عَبَسَ وَبَسَرَ ﴿٢٢﴾ ثُمَّ أَدْبَرَ وَٱسْتَكْبَرَ ﴿٢٣﴾ فَقَالَ إِنْ هَٰذَآ إِلَّا سِحْرٌ
يُؤْثَرُ ﴿٢٤﴾ إِنْ هَٰذَآ إِلَّا قَوْلُ ٱلْبَشَرِ ﴿٢٥﴾ سَأُصْلِيهِ سَقَرَ ﴿٢٦﴾ وَمَآ أَدْرَىٰكَ
مَا سَقَرُ ﴿٢٧﴾ لَا تُبْقِى وَلَا تَذَرُ ﴿٢٨﴾ لَوَّاحَةٌ لِّلْبَشَرِ ﴿٢٩﴾ عَلَيْهَا تِسْعَةَ عَشَرَ
﴿٣٠﴾ وَمَا جَعَلْنَآ أَصْحَٰبَ ٱلنَّارِ إِلَّا مَلَٰٓئِكَةً ۙ وَمَا جَعَلْنَا عِدَّتَهُمْ إِلَّا فِتْنَةً
لِّلَّذِينَ كَفَرُوا۟ لِيَسْتَيْقِنَ ٱلَّذِينَ أُوتُوا۟ ٱلْكِتَٰبَ وَيَزْدَادَ ٱلَّذِينَ ءَامَنُوٓا۟ إِيمَٰنًا ۙ
وَلَا يَرْتَابَ ٱلَّذِينَ أُوتُوا۟ ٱلْكِتَٰبَ وَٱلْمُؤْمِنُونَ ۙ وَلِيَقُولَ ٱلَّذِينَ فِى قُلُوبِهِم مَّرَضٌ
وَٱلْكَٰفِرُونَ مَاذَآ أَرَادَ ٱللَّهُ بِهَٰذَا مَثَلًا ۚ كَذَٰلِكَ يُضِلُّ ٱللَّهُ مَن يَشَآءُ وَيَهْدِى
مَن يَشَآءُ ۚ وَمَا يَعْلَمُ جُنُودَ رَبِّكَ إِلَّا هُوَ ۚ وَمَا هِىَ إِلَّا ذِكْرَىٰ لِلْبَشَرِ ﴿٣١﴾ كَلَّا
وَٱلْقَمَرِ ﴿٣٢﴾ وَٱلَّيْلِ إِذْ أَدْبَرَ ﴿٣٣﴾ وَٱلصُّبْحِ إِذَآ أَسْفَرَ ﴿٣٤﴾ إِنَّهَا لَإِحْدَى
ٱلْكُبَرِ ﴿٣٥﴾ نَذِيرًا لِّلْبَشَرِ ﴿٣٦﴾ لِمَن شَآءَ مِنكُمْ أَن يَتَقَدَّمَ أَوْ يَتَأَخَّرَ ﴿٣٧﴾ كُلُّ
نَفْسٍۭ بِمَا كَسَبَتْ رَهِينَةٌ ﴿٣٨﴾ إِلَّآ أَصْحَٰبَ ٱلْيَمِينِ ﴿٣٩﴾ فِى جَنَّٰتٍ يَتَسَآءَلُونَ
﴿٤٠﴾ عَنِ ٱلْمُجْرِمِينَ ﴿٤١﴾ مَا سَلَكَكُمْ فِى سَقَرَ ﴿٤٢﴾ قَالُوا۟ لَمْ نَكُ مِنَ
ٱلْمُصَلِّينَ ﴿٤٣﴾ وَلَمْ نَكُ نُطْعِمُ ٱلْمِسْكِينَ ﴿٤٤﴾ وَكُنَّا نَخُوضُ مَعَ
ٱلْخَآئِضِينَ ﴿٤٥﴾ وَكُنَّا نُكَذِّبُ بِيَوْمِ ٱلدِّينِ ﴿٤٦﴾ حَتَّىٰٓ أَتَىٰنَا ٱلْيَقِينُ ﴿٤٧﴾

zowawa za chilango ndi mavuto opanda mpumulo kwa amenewo kwa iye.( Amene amatchulidwayu apa ndi Al Waliid Bun Al Muhgiirah amene adali wamankhalu ku choonadi, wolimbana ndi Allah ndi Mtumiki Wake (SAW), ndipo iyi ndiyo mphoto ya munthu aliyense wochitira mankhalu choonadi nachisiya.]

(18) Iye adalingalira (mu mtima mwake) ndi kukonza bwino (chonena chonyoza Qur'aan).

(19) Choncho waonongeka! Adakonza bwanji (poinyoza Qur'aan)!

(20) Ndiponso waonongeka! Adakonza bwanji (poinyoza Qur'aan).

(21) Kenako adayang'ana (nkhope za anthu).

(22) Kenakonso adachita tsinya nkhope (kwambiri ndi mkwiyo).

(23) Kenakanso adanyoza choonadi ndi kudzikweza (posachivomera).

(24) Adati: "Sichina ichi (zimene wadza nazo Muhammad SAW) koma ndi matsenga amene adayamba kalekale kuphunzitsidwa (kuchokera kwa amatsenga akale).

(25) "Sichina ichi koma amatsenga ndi mawu a anthu!

18- 25 [Ndithu iyeyu adaganiza mu mtima mwake ndipo adakonza zomwe anganene mu zonyoza za Muhammad (SAW) ndi Qur'aan ndiye adatembereredwa, ndikuyenerera ndi zimenezo chionongeko. Adakonza motani mu mtima mwake m'nyozo umenewu? Kenako adatembereredwa. Kenako adaganiza mu zomwe adakonza ndi kuzilinganiza zonyoza Qur'aan, ndipo kenako adakwinya nkhope yake ndipo adalimbikira pochita tsinya lam'nanu pamene adabanika iye kusowa chochita ndikuti sadapeze chonyozera Qur'aan. Kenako adabwerera uku akutembenuka kusiya choonadi nadzikuza kusiya kuivomereza nati: "Izi zomwe akuyankhulazi Muhammad sichina koma ufiti umene ukumatengedwa kuchokera kwa anthu oyambirira mosiiranasiirana. Amenewa sichina kupatula kuti ndi mawu a zolengedwa zimene waziphunzira Muhammad (SAW) kuchokera kwa iwo kenako nadzikundikira iyeyo zimenezo kuti ndi zochokera kwa Allah.]

(26) Posachedwa ndim'lowetsa ku moto.

(27) Nanga ndi chiyani chikudziwitsa za moto?

(28) Siutsalitsa (mnofu) ndiponso susiya (fupa).

(29) Umapsereza ndi kudetsa khungu.

(30) (Kumeneko) kuli khumi ndi asanu ndi anayi (alonda oyang'anaira motowo).

26-30 [Ndikamulowetsa ku jahena kuti akalowe mu kuotcha kwake ndikupserera ndi moto wakewo. Ndi chinthu chanji chikudziwitse za moto umenewo? Umenewo siusiya m'nofu ngakhalenso fupa pokhapokha utaziotcha nkusandutsa khungu,kulidetsa ndi kulipsereza. Akuyang'anira za motowo ndi kumapereka chilango kwa anthu okhala m'menemo, ndi angero okwanira khumi ndi asanu ndi anayi (19) mwa angero olondera moto amphamvu kwambiri.]

(31) Ndipo sitidaike oyang'anira ku moto (kukhala anthu) koma angero; ndipo sitidaike chiwerengero chawo koma ndi mayeso kwa amene sadakhulupirire, ndi kuti atsimikize amene adapatsidwa mabuku (zimene Qur'aan ikunena za chiwerengero cha angero a ku moto) ndiponso kuti chionjezereke chikhulupiriro kwa amene akhulupirira, ndikuti asapeneke amene adapatsidwa mabuku pamodzi ndi okhulupirira. Ndiponso kuti anene amene m'mitima mwawo muli matenda (achinyengo) komanso osakhulupirira kuti: "Kodi Allah akulinganji pa fanizo limeneli?" Momwemo Allah akum'lekerera kusokera amene wam'funa ndipo akumuongola amene wam'funa. Ndipo palibe amene angadziwe magulu a nkhondo a Mbuye wako kupatula Iye. (Kutchula moto ndi za m'kati mwake) sichina koma ndi chenjezo kwa anthu.

[Ndipo sitidawaike olondera moto (kukhala anthu

wamba) kupatula kuti ndi angero ouma mitima. Ndipo sitidaike chiwerengero chimenecho kupatula kuti ndi mayeso kwa anthu amene adakanira Allah. Ndikuti papezeke chitsimikizo kwa anthu amene adapatsidwa mabuku kale mwa Ayuda ndi Akhristu kuti ndithu zimene zadza mu Qur'aan zokhudzana alonda a ku jahena, ndithudi ndi zoona zochokera kwa Allah ,popeza zalingana ndi mabuku awo. Ndikutinso awonjezereke anthu okhulupirira kumuvomereza Allah. Mtumiki Wake (SAW) ndi kugwiritsira ntchito malamulo Ake. Ndikuti asamakaike anthu amene adapatsidwa Buku mwa Ayuda ndi Akhristu ngakhalenso anthu okhulupirira mwa Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) . ndikuti aziyankhula anthu amene m'mitima mwawo muli uchiphamaso komanso makafiri kuti: "Kodi Allah amafunanji ndichiwerengero chodabwitsachi?" Zofanana ndi zomwe zatchulidwazi Allah amalekerera kusokera kwa amene wam'funa kumusokeretsa ndipo amaongola amene wafuna kuwaongola, palibe amene akudziwa (chiwerengero) cha asirikali a Mbuye wako mwa angero kupatula Allah Yekhayo. Ndipo moto siuli china chilichonse kupatula chikumbutso ndi ulaliki kwa anthu.]

32 Sichoncho, ndikulumbirira mwezi.

33 Ndi usiku pamene ukuchoka.

34 Ndi m'bandakucha pamene kukuwala.

35 Ndithu uwo (moto wa jahena) ndi chimodzi mwa malodza aakulu.

37 Ndi chenjezo kwa anthu,

36 Kwa yemwe wafuna mwa inu kutsogola (pochita zabwino zokam'thandiza tsiku louka kwa akufa) kapena kutsalira (ndi za m'dziko).

32-37 [Zinthu sikuti zili monga m'mene atchulira mu zokanira Mtumiki (SAW) mu zomwe wadza nazo. Allah walumbirira mwezi ndi usiku pamene ukupita ndi kuchoka ndi kum'bandakucha kukamayera nkuwonekera. Ndithu moto ndi chimodzi mwa zinthu zikuluzikulu; kuchenjeza ndi kuopseza anthu; kwa amene akufuna mwa inu kuti adziyandikitse kwa Mbuye wake kudzera mukuchita zomumvera, kapena amene wafuna kutsalira pochita za machimo.]

38 Mzimu uliwonse ukakhala chikole ndi zimene udachita.

39 Kupatula a kudzanja lamanja (Asilamu amene adadzimasula okha potembenukira kwa Allah).

40 (Iwo) adzakhala m'minda (yosasimbika kukongola kwake) akufunsana wina ndi mnzake.

41 Za anthu oipa

42 (Kuti): "N'chiyani chakulowetsani ku moto?"

43 Adzanena : "Sitidali m'gulu la omwe adali kupemphera (swalaat).

44 "Ndiponso sitidali kuwadyetsa masikini.

45 " Koma tinkangomira (m'zachabe ndi zabodza) pamodzi ndi omira m'menemo

46 "Ndiponso tidali kukana za tsiku la malipiro.

47 "Mpaka imfa idatifika".

38-47 [Mzimu uliwonse zimene udachita mu ntchito zoipa ali omangika ndi kuchitidwa chikole nazo pochita zimenezo, sakamasulidwa kufikira atakapereka zoyenerera zake mu zinthu zofunikira kubwezera kwa anthu amene adawachitira komanso chilango. Kupatula Asilamu odziyeretsa eni ku dzanja lakumanja amene adamasula makosi awo ndi kumvera (Allah) , iwo akakhala m'minda yomwe mbiri zake nkosatheka kuzitchula ndikuzifikira. Iwo azikafunsana wina ndi mnzake za anthu okanira (makafiri) amene adalakwa mu zinthu zokhudza eni akewo kuti: "Kodi ndi chiyani chakulowetsani mu jahena ndi chimene chakuchititsani kuti muzilawa kuotcha kwake?" Anthu oipawa akanena kuti: "Sitidali mu gulu la anthu opemphera swalaat pa dziko lapansi, ndipo sitidali kupereka sadaka kwa anthu ovutika ndi osowa, ndipo tidali kuyankhula nkhani zabodza limodzi ndi anthu opotoka ndi kusokera, ndipo tidali kulikanira tsiku la chiwerengero cha ntchito zathu ndi malipiro kufikira idatidzera imfa ife tili mu kusokera kumeneko ndi zinthu zoipazo.]

48 Siudzawathandiza uwomboli wa aomboli.

[Ndipo silidzawathandiza pempho la uomboli wa aomboli onse mwa angero, aneneri ndi ena otero chifukwa pempho la uomboli ndithudi limakhala kwa amene Allah wasangalatsidwa naye ndi kuvomereza kumupemphera pempholo.]

49 Kodi ali ndi chiyani iwo pakuti azinyozera chenjezoli (limene lili Qur'aan)?

1 50 (Akuyenda mothamanga kuti asamve chenjezoli) ngati kuti iwo ndi mbidzi zothawa.

2 51 (Zimene) zathawa mkango.

49-51 [Bwanji anthu opembedza mafanowa akumaichokera, kuipatsa msana Qur'aan ndi zimene zili m'menemo mu za ulaliki? Kukhala ngati iwowo ndi abulu a m'tchire kuthawa kwambiri zomwe zathawa mkango wolusa kwambiri].

52 Ati akufuna aliyense mwa iwo apatsidwe kalata zotambasulidwa (zimene zitsimikize uthenga wa Mneneri Muhammad (SAW).

53 Sichoncho! Koma kuti iwo sakuopa Tsiku Lomaliza.

54 Sichoncho! Ndithu ichi (Qur'aan) ndi chikumbutso (chokwanira)

فَمَا تَنفَعُهُمْ شَفَٰعَةُ ٱلشَّٰفِعِينَ ﴿٤٨﴾ فَمَا لَهُمْ عَنِ ٱلتَّذْكِرَةِ مُعْرِضِينَ
﴿٤٩﴾ كَأَنَّهُمْ حُمُرٌ مُّسْتَنفِرَةٌ ﴿٥٠﴾ فَرَّتْ مِن قَسْوَرَةٍۭ ﴿٥١﴾ بَلْ يُرِيدُ
كُلُّ ٱمْرِئٍ مِّنْهُمْ أَن يُؤْتَىٰ صُحُفًا مُّنَشَّرَةً ﴿٥٢﴾ كَلَّا ۖ بَل لَّا يَخَافُونَ
ٱلْءَاخِرَةَ ﴿٥٣﴾ كَلَّآ إِنَّهُۥ تَذْكِرَةٌ ﴿٥٤﴾ فَمَن شَآءَ ذَكَرَهُۥ ﴿٥٥﴾
وَمَا يَذْكُرُونَ إِلَّآ أَن يَشَآءَ ٱللَّهُ ۚ هُوَ أَهْلُ ٱلتَّقْوَىٰ وَأَهْلُ ٱلْمَغْفِرَةِ ﴿٥٦﴾

ترتيبها ٧٥ — سُورَةُ القِيَامَةِ — آياتها ٤٠

بِسْمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحْمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

لَآ أُقْسِمُ بِيَوْمِ ٱلْقِيَٰمَةِ ﴿١﴾ وَلَآ أُقْسِمُ بِٱلنَّفْسِ ٱللَّوَّامَةِ ﴿٢﴾ أَيَحْسَبُ
ٱلْإِنسَٰنُ أَلَّن نَّجْمَعَ عِظَامَهُۥ ﴿٣﴾ بَلَىٰ قَٰدِرِينَ عَلَىٰٓ أَن نُّسَوِّىَ بَنَانَهُۥ ﴿٤﴾ بَلْ
يُرِيدُ ٱلْإِنسَٰنُ لِيَفْجُرَ أَمَامَهُۥ ﴿٥﴾ يَسْـَٔلُ أَيَّانَ يَوْمُ ٱلْقِيَٰمَةِ ﴿٦﴾ فَإِذَا بَرِقَ ٱلْبَصَرُ
﴿٧﴾ وَخَسَفَ ٱلْقَمَرُ ﴿٨﴾ وَجُمِعَ ٱلشَّمْسُ وَٱلْقَمَرُ ﴿٩﴾ يَقُولُ ٱلْإِنسَٰنُ يَوْمَئِذٍ
أَيْنَ ٱلْمَفَرُّ ﴿١٠﴾ كَلَّا لَا وَزَرَ ﴿١١﴾ إِلَىٰ رَبِّكَ يَوْمَئِذٍ ٱلْمُسْتَقَرُّ ﴿١٢﴾ يُنَبَّؤُا۟ ٱلْإِنسَٰنُ
يَوْمَئِذٍۭ بِمَا قَدَّمَ وَأَخَّرَ ﴿١٣﴾ بَلِ ٱلْإِنسَٰنُ عَلَىٰ نَفْسِهِۦ بَصِيرَةٌ ﴿١٤﴾ وَلَوْ أَلْقَىٰ
مَعَاذِيرَهُۥ ﴿١٥﴾ لَا تُحَرِّكْ بِهِۦ لِسَانَكَ لِتَعْجَلَ بِهِۦٓ ﴿١٦﴾ إِنَّ عَلَيْنَا جَمْعَهُۥ
وَقُرْءَانَهُۥ ﴿١٧﴾ فَإِذَا قَرَأْنَٰهُ فَٱتَّبِعْ قُرْءَانَهُۥ ﴿١٨﴾ ثُمَّ إِنَّ عَلَيْنَا بَيَانَهُۥ ﴿١٩﴾

(55) Amene wafuna akumbukira (amene sakufuna ndi zake).

(56) Ndipo sangakumbukire pokhapokha Allah atafuna. Iye ndiye Amene ali Woyenera kumuopa, ndiponso ndiye Mwini kukhululuka (kwa amene akumuopa).

52-56 [Zoonadi, ndithu Quran ndi ulaliki ozama okwanira kuti iwo alangizidwire nawo. Amene akufuna kulangizika , alangizidwa ndi zomwe zili m'menemo ndikuthandizika ndi chiongolo chake. Palibe amene angalangizidwe nayo kupatula atamufunira Allah chiongoko. Ndipo Iye Subhaanahu ndi Mwini Woyenerera kuti adziopedwa ndi kumveredwa, komanso ndi Mwini Woti n'kukhululukira yemwe wamukhulupirira Iye ndikumumvera.]

## (75) SUURAT –UL- QIYAAMAT

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Ndikulumbirira Tsiku Lachimaliziro.

(2) Ndikulumbiriranso mzimu wodzidzudzula (pa cholakwa chimene wachita; ndithu, m'dzaukitsidwa, mafupa anu omwazikana atasonkhanitsidwa).

(3) Kodi munthu akuganiza kuti Ife (Amene tidam'lenga kuchokera kopanda chilichonse) sitidzatha kusonkhanitsa mafupa ake (ofumbwa)?

(4) Iyayi, Ife tikhoza (kutisonkhanitsa) ndi kutilongosola bwino timizere takunsonga kwa zala zake (mafupa ake ndiye osanena).

1-4 [Allah walumbirira tsiku la chiwerengero ndi malipiro. Ndiponso walumbirira mzimu wokhulupirira woopa umene umamudzudzula mwini wakeyo posiya zomvera Allah ndi kuchita zinthu zomugwetsera m'mavuto. Ndithudi anthu adzaukitsidwa kwa akufa. Kodi akuganiza kafiri kuti Ife sitidzatha kusonkhanitsa mafupa ake pambuyo potayanatayana? Iyayi, sichoncho, koma kuti Ife ndi Wokhoza kuti tisonkhanitse zala zake kapena nsonga zake pambuyo powasonkhanitsa ndi kuwaluzanitsa kukhala cholengedwa chalungalunganso monga m'mene chinalili asadafe.]

(5) Koma munthu akukanira (kuukaku) n'cholinga chopitiriza kuchita zoipa m'masiku omwe akudza mtsogolo mwa moyo wake onse.

(6) Akufunsa (mwa chipongwe): "Kodi lidzakhala liti tsiku lachimaliziro?"

[Koma munthu akukanira kuuka kwa akufa. Akufuna kukhalabe pa kuipitsa mu zomwe zili n'kudza mu masiku a moyo wake. Akumafunsa kafiri ameneyu motalikitsa kuti sizingachitike za kufika kwa Kiyama: "Kodi Kiyama idzabwera liti?"

(7) Pamene maso adzangoti tong'oo (ndi mantha).

(8) Ndi kuchoka kuwala kwa mwezi.

(9) Ndipo dzuwa ndi mwezi ndikusonkhanitsidwa (potuluka ku zambwe).

(10) Munthu adzanena tsiku limenelo: " Nkuti kothawira (chilangochi)?"

(11) (Adzauzidwa): "Iyayi, (iwe munthu) palibe pothawira (pako).

(12) Tsiku limenelo kobwerera (anthu) ndi kwa Mbuye wako.

7-12 [Zinthu sizili monga m'mene ukulakalakalira iwe munthu -mu zofuna kuthawa- palibe kothawira kapena kopulumukira kwina. Kwa Allah Yekhayo ndiko mudzabwerere zolengedwa zonse Tsiku Lakiyama ndipo ndi kokhazikaka kwawo, ndikudzalipidwa aliyense zimene zikumuyenerera].

(13) Tsiku limenelo munthu adzauzidwa zochita zake zimene adazitsogoza ndi zimene adazichedwetsa.

(14) Koma munthu adzadzichitira umboni yekha pa mzimu wake.

(15) Ngakhale atapereka madandaulo ake (chotani kuti apulumuke nawo sadzapulumuka).

13-15 [Koma munthu ndi umboni woonekeratu pa mzimu wake womwe adzakhala nawo

osam'taya pa zinthu zimene adazichita kapena kuzileka. Angakhale atabweretsa madandaulo ena aliwonse wodandaulira nawo kulakwa kwake, ndithu iyeyo sizidzamuthandiza zimenezo.]

16 Usaigwedezere (Qur'aan) lirime lako (pamene ikuvumbulutsidwa) kuti uifulumizitsire (kuiwerenga ndi kuisunga mu mtima).

17 Ndithu, ndi udindo Wathu kuisonkhanitsa (mu mtima mwako) ndi kuikhazikitsa kawerengedwe kake (pa lirime lako).

18 Pamene tikukuwerengera iwe tsatira kuwerenga kwakeko (uku uli chetee).

19 Kenako, ndithu, ndi udindo Wathu kuilongosola (zimene sukumvetsa).

16- 19 [Usagwedeze iwe Mneneri (SAW) lirime lako ndi Qur'aan pa nthawi imene chivumbulutso chikutsika ndi cholinga choti uifulumizitsire kuisunga kwake kuopa kukuthawira iweyo. Ndithu ndi zofunika kwa Ife kuisonkhanitsa mu mtima mwako kenako kuti uziiwerenga ndi lirime lako momwe ungafunire. Ngati Mtumiki Wathu Jibril (AS) atakuwerengera iweyo, mvetsera kuwerenga kwake ndipo cheteka kwa iye. Kenako uiwerenge monga m'mene wakuwerengerera iyeyo. Kenako ndi udindo Wathu kulongosola zimene zakuvuta kuzimvetsa mu matanthauzo ake komanso malamulo ake.]

20 Ayi, sidero , koma mukukondetsetsa zofulumira (za moyo wa dziko lapansili).

21 Ndipo mukusiya (moyo wa) Tsiku Lomaliza.

20-21 [Zinthu sizili monga mukunenera inu anthu opembedza mafano zakuti kulibe kuuka kwa akufa komanso malipiro, koma kuti inu ndi anthu okondetsetsa dziko lapansi ndi zokongoletsa zake ndipo mukusiya Tsiku Lomaliza ndi mtendere wake.]

22 Nkhope zina tsiku limenelo zidzawala kwambiri (ndi mtendere).

23 Zili kumuyang'ana Mbuye wawo.

22-23 [Nkhope za anthu achisangalalo Tsiku Lakiyama zidzakhala zokongola za mtendere zikumuona Mlengi wawo ndi Mwini nkhopezo ndipo zidzasangalala ndi zimenezo.]

24 Ndipo nkhope zina tsiku limenelo zidzakhala zokhwinyata.

25 Zikuyembekezera kuti zilandira tsoka lodula msana.

24- 25 [Ndipo nkhope za anthu oipa Tsiku Lakiyama zidzakhala zokhwinyata, zatsinya, zikuyembekezera kuti vuto lalikulu zedi lodula msana lizigwera]

26 Sichoncho! Pamene mzimu udzafika pa nthiti za mtima,

كَلَّا بَلۡ تُحِبُّونَ ٱلۡعَاجِلَةَ ﴿٢٠﴾ وَتَذَرُونَ ٱلۡأٓخِرَةَ ﴿٢١﴾ وُجُوهٞ يَوۡمَئِذٖ نَّاضِرَةٌ ﴿٢٢﴾
إِلَىٰ رَبِّهَا نَاظِرَةٞ ﴿٢٣﴾ وَوُجُوهٞ يَوۡمَئِذِۭ بَاسِرَةٞ ﴿٢٤﴾ تَظُنُّ أَن يُفۡعَلَ بِهَا فَاقِرَةٞ ﴿٢٥﴾
كَلَّآ إِذَا بَلَغَتِ ٱلتَّرَاقِيَ ﴿٢٦﴾ وَقِيلَ مَنۡۜ رَاقٖ ﴿٢٧﴾ وَظَنَّ أَنَّهُ ٱلۡفِرَاقُ ﴿٢٨﴾ وَٱلۡتَفَّتِ
ٱلسَّاقُ بِٱلسَّاقِ ﴿٢٩﴾ إِلَىٰ رَبِّكَ يَوۡمَئِذٍ ٱلۡمَسَاقُ ﴿٣٠﴾ فَلَا صَدَّقَ وَلَا صَلَّىٰ
﴿٣١﴾ وَلَٰكِن كَذَّبَ وَتَوَلَّىٰ ﴿٣٢﴾ ثُمَّ ذَهَبَ إِلَىٰٓ أَهۡلِهِۦ يَتَمَطَّىٰٓ ﴿٣٣﴾ أَوۡلَىٰ لَكَ
فَأَوۡلَىٰ ﴿٣٤﴾ ثُمَّ أَوۡلَىٰ لَكَ فَأَوۡلَىٰٓ ﴿٣٥﴾ أَيَحۡسَبُ ٱلۡإِنسَٰنُ أَن يُتۡرَكَ سُدًى ﴿٣٦﴾
أَلَمۡ يَكُ نُطۡفَةٗ مِّن مَّنِيّٖ يُمۡنَىٰ ﴿٣٧﴾ ثُمَّ كَانَ عَلَقَةٗ فَخَلَقَ فَسَوَّىٰ ﴿٣٨﴾ فَجَعَلَ مِنۡهُ
ٱلزَّوۡجَيۡنِ ٱلذَّكَرَ وَٱلۡأُنثَىٰٓ ﴿٣٩﴾ أَلَيۡسَ ذَٰلِكَ بِقَٰدِرٍ عَلَىٰٓ أَن يُحۡـِۧيَ ٱلۡمَوۡتَىٰ ﴿٤٠﴾

ترتيبها ٧٦ — **سُورَةُ الإِنسَانِ** — آياتها ٣١

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

هَلۡ أَتَىٰ عَلَى ٱلۡإِنسَٰنِ حِينٞ مِّنَ ٱلدَّهۡرِ لَمۡ يَكُن شَيۡـٔٗا مَّذۡكُورًا ﴿١﴾
إِنَّا خَلَقۡنَا ٱلۡإِنسَٰنَ مِن نُّطۡفَةٍ أَمۡشَاجٖ نَّبۡتَلِيهِ فَجَعَلۡنَٰهُ سَمِيعَۢا
بَصِيرًا ﴿٢﴾ إِنَّا هَدَيۡنَٰهُ ٱلسَّبِيلَ إِمَّا شَاكِرٗا وَإِمَّا كَفُورًا ﴿٣﴾
إِنَّآ أَعۡتَدۡنَا لِلۡكَٰفِرِينَ سَلَٰسِلَاْ وَأَغۡلَٰلٗا وَسَعِيرًا ﴿٤﴾ إِنَّ
ٱلۡأَبۡرَارَ يَشۡرَبُونَ مِن كَأۡسٖ كَانَ مِزَاجُهَا كَافُورًا ﴿٥﴾

27 Ndipo ndikunenedwa kuti: "Ndani angam'chiritse?"

28 Ndipo iye (mwini wake) ndithu, n'kutsimikiza kuti uku n'kusiyana (ndi dziko lapansi lomwe lidali lokondedwa kwa iye).

29 Ndipo miyendo idzasanjikizana (pamenepo n'kuti atapezeka pa nthawi yochoka mzimu).

30 Tsiku limenelo koperekedwa (anthu onse) ndi kwa Mbuye wako.

26- 30 [Zoonadi! Ukafika mzimu kumwamba kwa chidali, ena amene ali pamenepo nanena kuti: "Kodi pali sing'anga woti amuchitire mankhwala ndi kumuchiza m'zomwe ali nazozi?" ndipo natsimikiza munthu amene yamufikira imfayo kuti zomwe zamupezazi ndi kusiyana ndi dziko lapansi chifukwa cha kuwaona kwake angero a imfa. Komanso nkulumikizana mavuto a mapeto a dziko lapansi ndi mavuto a kuyamba kwa Tsiku Lomaliza. Kwa Allah ndiko kosakiridwa akapolo onse Tsiku Lakiyama, mwina ku jannah kapena ku moto].

31 Ndipo sadakhulupirire komanso sadapemphere swalaat (zisanu)

32 Koma (m'malo mwake) adatsutsa ndi kunyoza.

33 Kenako adapita ku banja lake (uku akuyenda) monyada.
34 Kuonongeka nkwako (iwe wotsutsa)! Kuonongeka zedi!
35 Ndiponso kuonongeka ndi kwako! Kuonongeka ndi kwako!

31-35 [Kafiri sadakhulupirire Mtumiki (SAW) ndi Qur'aan komanso sadamuchitire Allah swalaat zisanu zokakamiza. Koma adakanira Qur'aan komanso adatembenuka kuchipatsa msana chikhulupiriro. Kenako adapita ku banja kwake mothimbwidzika akudzikweza mayendedwe ake. Kuonongeka nkwako kuonongeka nkwako kenakonso kuonongeka nkwako kuonongeka nkwako.]

36 Kodi munthu (wotsutsa za kuukayu) akuganiza kuti angosiidwa chabe (popanda kuweruzidwa pa zochita zake ndi kuti Allah sadam'kakamize malamulo ofunika kuwatsata)?
37 Kodi sadali dontho la umuna umene udafwamphukira (m'chibereko)?
38 Kenako adakhala ntchintchi ya magazi, ndipo adam'lenga ndi kum'linganiza (monga munthu),
39 Ndipo adalenga kuchokera m'menemo (m'magazi) omwewo mitundu iwiri, mwamuna ndi mkazi.
40 Kodi (iye amene adayambitsa chilengedwe choyambachi) sangathe kuwapatsa moyo akufa?

36-40 [Kodi wokanirayu za kuuka kwa akufa akuganiza kuti angathe kungosiidwa chabe popanda kulamulidwa malamulo ndi kuletsedwa komanso osamuwerengera zochita zake kapena kulangidwa? Kodi munthu ameneyu sadali dontho lofooka la umuna lochokera ku madzi achabechabe oyaluka othiridwa ndi kufwamphukira mu ziberekero, kenaka nakhala ntchintchi ya magazi ouma, ndipo Allah namulenga kudzera mu kukhoza Kwake nawalinganiza maonekedwe ake kulinganiza kwabwino? Ndipo adachita kuchokera kwa munthu ameneyu mitundu iwiri; mwamuna ndi mkazi. Kodi Wopembedzedwa Ameneyu, Mlengi wa zinthu zimenezi siwokhoza kubwezeretsa zolengedwa pambuyo pa kutha kwawo? Indedi ndithu Iye Subhaanahu ndi Wokhoza pa zimenezo.]

## (76) SUURAT –UL –AD'DAHR

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Ndithu, munthu idam'pita nthawi yaitali kwambiri (asanauziridwe mzimu) pomwe sadali chinthu chotchulidwa.

[Ndithudi idamudutsa munthu nthawi yaitali ya m'nyengo usanauziridwe mzimu mwa iye, sadali kanthu koti n'kutchulidwa ndipo siinkadziwika mbuto yake].

2 Ndithu, Ife tam'lenga munthu kuchokera ku mbewu ya umunthu yosakanikirana (ya mkazi ndi ya mwamuna) kuti timuyese mayeso ( ndi malamulo Athu) choncho tidam'panga kukhala wakumva ndi wopenya (amve mawu a Allah ndikuti aone zisonyezo Zake).
3 Ife tidam'longosolera njira yoongoka kukhala wokhulupirira kapena wotsutsa (zonse zili kwa iye).

2-3 [Nidthu Ife tidamulenga munthu kuchokera ku mbewu ya umunthu yosakanikirana kuchokera ku madzi a mwamuna ndi a mkazi. Pambuyo pake timamuyesa ndi malamulo nkumuchita kukhala wakumva ndi kupenya kuti adzimva ma Ayah ndi kumaona zisonyezo. Ndithu Ife tamulongosolera ndi kumuonetsera njira ya chiongoko ndi chisokonezo komanso chabwino ndi choipa kuti akhale mwina wokhulupirira, woyamika kapena wokanira, wamankhalu.]

4 Ndithu, Ife okana tawakonzera unyolo (wam'miyendo yawo) ndi magoli (a m'manja ndi m'makosi awo) ndi moto waukali woyaka.

[Ndithu Ife tawakonzera anthu okanira maunyolo a chitsulo amene akamangidwe nawo miyendo yawo ndiponso magoli amene akamangidwe nawo manja awo ku makosi awo komanso moto umene akaotchedwe nawo.]

5 Ndithu, oona pa chikhulupiriro chawo adzamwa vinyo, chosakanizira chake chidzakhala (madzi) a kaafuura.

[Ndithudi eni kumvera (malamulo a Allah) ndi kudziyeretsa amene akuchita zoyenera kumuchitira Allah, azikamwa Tsiku Lakiyama kuchokera mu chikho momwe muli mowa wosakaniza ndi mtundu wonunkhira zabwino womwe ndi madzi a kaafuura.

6 (Kaafuura ameneyo) ndi kasupe amene azikamwamo akapolo a Allah ndi kum'tulutsa (paliponse pamene afuna) kum'tulutsa mofewa.
7 (Amene) akukwaniritsa zimene adalonjeza (okha kwa Allah), ndiponso akuopa tsiku (lalikulu) limene zoipa zake zidzakhala zofalikira ponseponse.
8 Ndipo amadyetsa chakudya masikini, amasiye ndi ogwidwa pa nkhondo, pomwe iwo akuchifunanso.
9 Amanena (cha mu mtima akamapereka chakudyacho): " Tikukudyetsani chifukwa chofuna chikondi cha Allah basi; sitikufuna kwa inu malipiro kapena kuthokoza.
10 Ndithu, ife tikuopa kwa Mbuye wathu tsiku lokhwinyata nkhope ndi mavuto aakulu.

6-10 [Chakumwa chimenechi chimene chasakanizidwa ndi kaafuura ndi mtsinje umene

azikamwa m'menemo akapolo a Allah, azikaona m'mene azikachitira momwe angafunire. Ndipo azikawayendetsa madzi a m'menemo kulikonse angakakufune kuyendetsa kosavuta. Iwowo ndi amene adali pa dziko lapansi akukwaniritsa zimene adazikakamiza okha mu zomvera Allah ndipo amaopa chilango cha Allah mu Tsiku Lakiyama chomwe zowawa zake zimakhala zoopsa komanso kuipa kwake ndi kofalikira, koyenderera kwa anthu kupatula amene Allah wamuchitira chisoni. Ndiponso amenewa amadyetsa chakudya ngakhale akuchikonda ndi kuchisowa munthu wosowa wolephera kugwira ntchchito amene alibiretu m'zinthu za pa dziko lapansi kalikonse, komanso mwana amene bambo ake adamwalira ndipo alibe chuma, komanso mkaidi wa pa nkhondo mwa anthu opembedza mafano ndi ena otero, ndipo akumanena m'mitima mwawo kuti: "Ndithudi tikukuchitirani zabwino pofuna chiyanjo cha Allah ndi kufuna malipiro Ake. Sitikufuna chosinthana m'malo mwake ndiponso sitikulinga chitamando kapena chiyamiko kuchokera kwa inu. Ndithu ife tikuopa kwa Mbuye wathu tsiku lovuta kwambiri lomwe nkhope zidzakhwinyate komanso kudzachita tsinya chifukwa cha kuopsa kwa tsikulo ndi kupweteka kwa mavuto ake.]

(11) Ndipo Allah adzawateteza ku mavuto a tsiku limenelo ndiponso adzawapatsa mtendere ndi chisangalalo.

(12) Ndipo adzawalipira chifukwa cha kupirira kwawo munda wa mtendere ndi nsalu za veleveti.

(13) Atatsamira m'menemo pa mabedi (a mtengo wapatali) sakamva m'menemo kutentha kwa dzuwa kapena kuzizira.

(14) Mithunzi yake ikawayandikira iwo ndipo mikoko ya zipatso idzatewa pafupi (moti munthu atha kuthyola ali chigonere).

11-14 [Ndipo Allah adzawateteza ku zopweteka za tsiku limenelo. Ndipo akawapatsa kukongola ndi kuwala pa nkhope zawo, komanso chisangalalo ndi chikondwerero m'mitima mwawo. Ndipo akawalipira chifukwa cha kupirira pa zakumvera Allah pa dziko lapansi, munda wa mtendere waukulu umene adzikadyamo m'mene angafunire. Komanso azikavala m'menemo nsalu ya veleveti, uku atatsamira m'menemo makama okongoletsedwa ndi nsalu ndi makatani a mtengo wapatali. Sakamva m'menemo kutentha kwa dzuwa kapena mphepo yozizira kwambiri. Ndipo mitengo yaku jannah izikawachitira mthunzi komanso kukafewetsedwa kotheratu kwa iwowo kuthyola zipatso m'menemo.]

عَيْنًا يَشْرَبُ بِهَا عِبَادُ ٱللَّهِ يُفَجِّرُونَهَا تَفْجِيرًا ﴿٦﴾ يُوفُونَ بِٱلنَّذْرِ وَيَخَافُونَ
يَوْمًا كَانَ شَرُّهُۥ مُسْتَطِيرًا ﴿٧﴾ وَيُطْعِمُونَ ٱلطَّعَامَ عَلَىٰ حُبِّهِۦ مِسْكِينًا
وَيَتِيمًا وَأَسِيرًا ﴿٨﴾ إِنَّمَا نُطْعِمُكُمْ لِوَجْهِ ٱللَّهِ لَا نُرِيدُ مِنكُمْ جَزَآءً وَلَا شُكُورًا
﴿٩﴾ إِنَّا نَخَافُ مِن رَّبِّنَا يَوْمًا عَبُوسًا قَمْطَرِيرًا ﴿١٠﴾ فَوَقَىٰهُمُ ٱللَّهُ شَرَّ ذَٰلِكَ
ٱلْيَوْمِ وَلَقَّىٰهُمْ نَضْرَةً وَسُرُورًا ﴿١١﴾ وَجَزَىٰهُم بِمَا صَبَرُوا۟ جَنَّةً وَحَرِيرًا
﴿١٢﴾ مُّتَّكِـِٔينَ فِيهَا عَلَى ٱلْأَرَآئِكِ ۖ لَا يَرَوْنَ فِيهَا شَمْسًا وَلَا زَمْهَرِيرًا ﴿١٣﴾
وَدَانِيَةً عَلَيْهِمْ ظِلَٰلُهَا وَذُلِّلَتْ قُطُوفُهَا تَذْلِيلًا ﴿١٤﴾ وَيُطَافُ عَلَيْهِم بِـَٔانِيَةٍ
مِّن فِضَّةٍ وَأَكْوَابٍ كَانَتْ قَوَارِيرَا۠ ﴿١٥﴾ قَوَارِيرَا۟ مِن فِضَّةٍ قَدَّرُوهَا تَقْدِيرًا ﴿١٦﴾
وَيُسْقَوْنَ فِيهَا كَأْسًا كَانَ مِزَاجُهَا زَنجَبِيلًا ﴿١٧﴾ عَيْنًا فِيهَا تُسَمَّىٰ سَلْسَبِيلًا
﴿١٨﴾ ۞ وَيَطُوفُ عَلَيْهِمْ وِلْدَٰنٌ مُّخَلَّدُونَ إِذَا رَأَيْتَهُمْ حَسِبْتَهُمْ لُؤْلُؤًا مَّنثُورًا
﴿١٩﴾ وَإِذَا رَأَيْتَ ثَمَّ رَأَيْتَ نَعِيمًا وَمُلْكًا كَبِيرًا ﴿٢٠﴾ عَٰلِيَهُمْ ثِيَابُ سُندُسٍ
خُضْرٌ وَإِسْتَبْرَقٌ ۖ وَحُلُّوٓا۟ أَسَاوِرَ مِن فِضَّةٍ وَسَقَىٰهُمْ رَبُّهُمْ شَرَابًا
طَهُورًا ﴿٢١﴾ إِنَّ هَٰذَا كَانَ لَكُمْ جَزَآءً وَكَانَ سَعْيُكُم مَّشْكُورًا ﴿٢٢﴾ إِنَّا
نَحْنُ نَزَّلْنَا عَلَيْكَ ٱلْقُرْءَانَ تَنزِيلًا ﴿٢٣﴾ فَٱصْبِرْ لِحُكْمِ رَبِّكَ وَلَا تُطِعْ
مِنْهُمْ ءَاثِمًا أَوْ كَفُورًا ﴿٢٤﴾ وَٱذْكُرِ ٱسْمَ رَبِّكَ بُكْرَةً وَأَصِيلًا ﴿٢٥﴾

(15) Ndipo akakhala akuzunguliridwa (ndi otumikira) uku atatenga zomwera za siliva ndi matambula onyezimira ndiponso olangala,

(16) Zolangala zopangidwa ku siliva, atalinga bwino zakumwazo (malinga ndi kufuna kwawo).

(17) Ndipo (anthu abwino) akamwetsedwa kumeneko vinyo chosakanizira chake zanjabiila (chikasu).

(18) M'menemo muli kasupe wotchedwa salisabila.

15-18 [Ndipo adzikawazungulirazungulira m'menemo otumkira ndi ziwiya za siliva za chakudya komanso ndi zikho za chakumwa kuchokera mu matambula ochokera ku siliva amene ayeza bwino opereka chakumwawo mofanana ndi chifuniro cha akumwawo osawonjezera kapena kupungula. Ndipo anthu abwino amenewa akamwetsedwa ku jannah ndi chikho chodzadza ndi mowa wosakanikizidwa ndi zanjabila. Azikamwa kuchokera ku mtsinje wa ku jannah wotchedwa Salisabila chifukwa ubwino wa chakumwa chake ndi kufewa kwa katsikidwe kake pa m'mero ndi ubwino wake.]

(19) Ndipo azikawazungulira anyamata (okongola) osasintha (chilengedwe chawo) utawaona (chifukwa cha kukongola kwawo ndi kuwala kwa nkhope zawo),

وَمِنَ ٱلَّيۡلِ فَٱسۡجُدۡ لَهُۥ وَسَبِّحۡهُ لَيۡلٗا طَوِيلًا ٢٦ إِنَّ
هَٰٓؤُلَآءِ يُحِبُّونَ ٱلۡعَاجِلَةَ وَيَذَرُونَ وَرَآءَهُمۡ يَوۡمٗا ثَقِيلٗا ٢٧ نَّحۡنُ
خَلَقۡنَٰهُمۡ وَشَدَدۡنَآ أَسۡرَهُمۡۖ وَإِذَا شِئۡنَا بَدَّلۡنَآ أَمۡثَٰلَهُمۡ تَبۡدِيلًا
٢٨ إِنَّ هَٰذِهِۦ تَذۡكِرَةٞۖ فَمَن شَآءَ ٱتَّخَذَ إِلَىٰ رَبِّهِۦ سَبِيلٗا ٢٩
وَمَا تَشَآءُونَ إِلَّآ أَن يَشَآءَ ٱللَّهُۚ إِنَّ ٱللَّهَ كَانَ عَلِيمًا حَكِيمٗا ٣٠
يُدۡخِلُ مَن يَشَآءُ فِي رَحۡمَتِهِۦۚ وَٱلظَّٰلِمِينَ أَعَدَّ لَهُمۡ عَذَابًا أَلِيمَۢا ٣١

## سُورَةُ المُرۡسَلَاتِ

ترتيبها ٧٧ — آياتها ٥٠

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

وَٱلۡمُرۡسَلَٰتِ عُرۡفٗا ١ فَٱلۡعَٰصِفَٰتِ عَصۡفٗا ٢ وَٱلنَّٰشِرَٰتِ نَشۡرٗا ٣
فَٱلۡفَٰرِقَٰتِ فَرۡقٗا ٤ فَٱلۡمُلۡقِيَٰتِ ذِكۡرًا ٥ عُذۡرًا أَوۡ نُذۡرًا ٦ إِنَّمَا
تُوعَدُونَ لَوَٰقِعٞ ٧ فَإِذَا ٱلنُّجُومُ طُمِسَتۡ ٨ وَإِذَا ٱلسَّمَآءُ فُرِجَتۡ
٩ وَإِذَا ٱلۡجِبَالُ نُسِفَتۡ ١٠ وَإِذَا ٱلرُّسُلُ أُقِّتَتۡ ١١ لِأَيِّ يَوۡمٍ أُجِّلَتۡ
١٢ لِيَوۡمِ ٱلۡفَصۡلِ ١٣ وَمَآ أَدۡرَىٰكَ مَا يَوۡمُ ٱلۡفَصۡلِ ١٤ وَيۡلٞ يَوۡمَئِذٖ
لِّلۡمُكَذِّبِينَ ١٥ أَلَمۡ نُهۡلِكِ ٱلۡأَوَّلِينَ ١٦ ثُمَّ نُتۡبِعُهُمُ ٱلۡأٓخِرِينَ
١٧ كَذَٰلِكَ نَفۡعَلُ بِٱلۡمُجۡرِمِينَ ١٨ وَيۡلٞ يَوۡمَئِذٖ لِّلۡمُكَذِّبِينَ ١٩

ungawaganizire kuti ndi ngale zomwazidwa. [Ndipo azikawazungulirazulngulira anthu abwino amenewa powatumikira anyamata osasintha maonekedwe awo. Utati uwaone, chifukwa cha kukongola kwawo ndi kuyera kwa mitundu yawo komanso kuwala kwa nkhope zawo, ungaganize kuti ndi ngale zowala zomwazidwa.]

(20) Ndipo ukadzaona (malo aliwonse ku jannah), ukaona kumeneko mtendere ndi ufumu waukulu. [Ukaona malo aliwonse mu jannah, uona m'menemo mtendere wosasimbika mbiri zake komanso ufumu waukulu wopanda malire.]

(21) Pamwamba pawo padzakhala nsalu za veleveti zopyapyala zobiriwira, ndi nsalu za velevete zotchindikala, akavekedwa m'manja mwawo zibangiri za siliva. Mbuye wawo akawamwetsa chakumwa china choyera kwambiri. [Pamwamba pawo ndipo matupi awo akanyamula zovala zomwe mkati mwake muli veleveti obiriwira opyapyala ndipo kunja kwake kopangidwa ndi veleveti wotchindikala. Akavekedwa ndi zokongoletsa za zibangiri za siliva, ndipo pamwamba pa zonsezi, Mbuye wawo akawamwetsa chakumwa chopanda kuipa mkati mwake kapena uve.]

(22) (Akawauza kuti): "Ndithu iyi ndi mphoto yanu; ndipo ntchito zanu ndi zolandiridwa. [Ndipo zikanenedwa kwa iwo kuti: "Ndithu izi zakonzedwera inu molingana ndi ntchito zanu zolungama, ndipo ntchito zanu pa dziko lapansi, kwa Allah ndi zokondweretsedwa zolandiridwa.)

(23) "Ndithu, Ife taivumbulutsa kwa iwe Qur'aan mwapang'onopang'ono (kuti uisunge bwino". [Ndithu Ife ndi Amene takuvumbulutsira iwe Mtumiki (SAW) Qur'aan chivumbulutso chochokera kwa Ife ndi cholinga choti uwakumbutse anthu zomwe zili m'menemo mu lonjezo, chiopsezo, malipiro ndi chilango.]

(24) Choncho, pirira ndi lamulo la Mbuye wako ndipo usam'vere wamachimo kapena wokanira aliyense mwa iwo.

(25) Ndipo kumbukira dzina la Mbuye wako m'mawa (pemphero swalaat ul Fajr) ndi madzulo (swalaat ya Zuhr ndi Asr).

24-25 [Pirira ndi lamulo la chikonzero cha Mbuye wako ndipo ulilandire , komanso lamulo Lake la chipembedzo ndipo uyendere limenelo., ndipo usamumvere wina aliyense mu anthu opembedza mafano amene wamira mu zilakolako kapena amene wapitiriza mu ukafiri ndi kusokera. Komanso upitirire potchula dzina la Mbuye wako ndi kumupempha kumayambiriro a tsiku komanso kumathero kwake.]

(26) Ndipo usiku m'lambire Iye (swalaat ya Maghrib ndi Isha) ndiponso umulemekeze usiku nthawi yaitali (popemphera sunnah ya Tahaj'jud). [Ndipo gawo la usiku ulambire Mbuye wako ndipo upemphere kwa Iye komanso uchite mapemphero a sunnah ya Tahaj'jud nthawi yaitali].

(27) Ndithu awa akukonda umoyo wa dziko lapansi, ndipo akulisiya kumbuyo kwawo tsiku lovuta. [Ndithu anthu opembedza mafanowa akukondetsetsa dziko lapansi n'kumatanganidwa nalo ndi kumasiya kumbuyo kwawo ntchito za Tsiku Lomaliza ndi zomwe zili m'menemo za chipulumutso chawo mu tsiku lalikulu mavuto ake.]

(28) Ife ndi Amene tidawalenga ndipo tidalimbika kalengedwe kawo ndipo titafuna tingabweretse ena onga iwo (omvera Allah) kulowa m'malo mwawo. [Ndithu Ife tidawalenga iwowo ndipo tidawalenga mwaluntha kwambiri kotero tikadafuna, tikadawaononga iwowo n'kubweretsa anthu omvera, otsatira malamulo a Mbuye wawo].

(29) Ndithu ichi ndi chikumbutso choncho amene afuna atsata njira yopitira kwa Mbuye wake (pomukhulupirira ndi kumumvera).

30 Koma simungafune nokha chilichonse pokhapokha atafuna Allah. Ndithu Allah Ngodziwa, Ngwanzeru.
31 Akam'lowetsa amene wam'funa ku chifundo Chake; koma oipa wawalinganizira chilango chowawitsa.
29-31 [Ndithu surah imeneyi ndi langizo kwa zolengedwa zonse, munthu amene wadzifunira yekha zabwino pa dziko lapansi ndi Tsiku Lomaliza, achita kudzera ku chikhulupiriro ndi kuopa njira yokam'fikitsa ku chikhululuko cha Allah ndi chiyanjo Chake. Ndipo palibe chomwe mungafune mu zinthu zili zonse pokhapokha zimakhala ndi chilinganizo cha Allah ndi chifuniro Chake. Ndithu Allah Ngodziwa bwino m'mene zilili zolengedwa Zake, Ngwanzeru zakuya pa kulinganiza Kwake komanso mu zochita Zake. Amamulowetsa amene wam'funa mwa akapolo Ake mu chifundo Chake ndi chiyanjo Chake- iwowa ndi amene ali okhulupirira. Ndipo wawakonzera anthu odumpha malire a Allah chilango chopweteka kwambiri].

## (77) SUURAT-UL- MURSALAAT

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Ndikulumbirira mphepo yomwe ikuomba motsatizana.
2 Ndikulumbirira mphepo yam'kuntho.
3 Ndi mphepo yobalalitsa mitambo ndi mvula.
4 Ndi ma Aayah osiyanitsa (pakati pa choona ndi chonama).
5 Ndi angero opereka chivumbulutso (kwa aneneri).
6 Kuti chichotse madandaulo ndiponso kuti chikhale chenjezo.
7 Ndithu zimene mukulonjezedwa (kuti chimaliziro chidzakhalapo) zidzachitikadi (popanda chikaiko).
1-7 [Allah walumbirira mphepo pamene ikuomba motsatizana ina pambuyo pa inzake, ndi mphepo ya m'kuntho imene ikuomba mwamphamvu moononga, ndi angero amene aikidwa kuti adziyendetsa mitambo nkuiyendetsa kupita nayo kumene Allah wafuna, ndi angero amene amatsika ndi zomwe zili kwa Allah zosiyanitsira pakati pa choona ndi chabodza komanso chololedwa ndi choletsedwa. Ndi angero amene akulandira chivumbulutso chochokera kwa Allah n'kumatsika nacho kwa aneneri Ake kuchotsa madandaulo kwa Allah kwa zolengedwa Zake ndi chenjezo kwa iwo kuti asadzakhale ndi chowiringula chili chonse. Ndithudi zimene mukulonjezedwa za Tsiku Lakiyama ndi zomwe zili m'menemo, mukuwerengedwa ntchito komanso malipiro, ndithu zidzachitika popanda chikaiko chilichonse].

8 Pamene nyenyezi zidzafafanizidwa (kuwala kwake ndi kuchotsedwa m'malo mwake).
9 Ndiponso pamene thambo lidzang'ambidwa ndi kutsekulidwa.
10 Ndi pamenenso mapiri adzachotsedwa m'malo mwake ndi kuperedwa (kukhala fumbi).
11 Ndi pamene aneneri adzasonkhanitsidwa pa nthawi yake (kuti apereke umboni ku mibadwo yawo).
12 Kodi ndi tsiku lanji adzichedwetsera (zinthu zikuluzikuluzo kuti zidzachitike).
13 Ndi tsiku la chiweruzo (pakati pa zolengedwa).
14 N'chiyani chakudziwitsa za tsiku la chiweruziro?
15 Kuonongeka kwakukulu tsiku limenelo kuli pa otsutsa (lonjezo Lathu la kuuka kwa akufa].
8-15 [Pamene nyenyezi zidzafafanizidwe ndi kuchoka kuwala kwake, ndi pamenenso thambo lidzang'ambidwe, komanso pamene mapiri adzaulutsidwe nkubalalikitsidwa nkukhala fumbi lowulutsidwa ndi mphepo, ndi pamenenso Atumuki adzapatsidwe nthawi ndi nyengo kuti zigamulidwe pakati pa iwo ndi mibadwo, kudzanenedwa: "Ndi tsiku lanji lomwe Atumiki achedwetseredwera?" Iwotu achedwetseredwa chifukwa cha tsiku la chigamulo ndi kusiyanitsa pakati pa zolengedwa. Iwe munthu chiti chikudziwitse kuti ndi chinthu chanji tsiku lachiweruzo ndi kupweteka kwa zoopsa zake? Chionongeko chachikulu tsiku limenelo kwa otsutsa].
16 Kodi sitidawaononge (anthu) akale (chifukwa cha machimo awo, monga a Nowa (AS) ,Adi ndi Samudu)?
17 Kenako titsatiza ena (okana Allah m'kuonongekako monga tidawachitira oyamba),
18 Chomwecho tiwachitiranso ochimwira (Allah).
16-18 [Kodi sitidawaononge oyambirira mu mibadwo imene idapita chifukwa chokanira kwawo Atumiki monga anthu a Nowa (AS), Aad ndi Samudu? Kenako titsatiza ndi iwowa atsopanowa mwa anthu amene anali ngati iwowo mu kukanira ndi kunyoza monga m'mene chinalili chionongeko choopsa ndi anthu oipa mwa makafiri a ku Makka chifukwa chokanira kwawo Mtumiki (SAW)].
19 Chilango chachikulu tsiku limenelo chili pa otsutsa (lonjezo Lathu la kuuka kwa akufa) [Chionongeko ndi chilango choopsa Tsiku Lakiyama chikakhala kwa aliyense wokanira zoti Allah Ndiye Wopembedzedwa mwachoonadi Iye Yekhayo Wopanda wophatikizana Naye, ndiponso uneneri, kuuka kwa akufa ndi chiwerengero cha ntchito za anthu].
20 Kodi sitidakulengeni kuchokera ku madzi

أَلَمْ نَخْلُقكُّم مِّن مَّآءٍ مَّهِينٍ ﴿٢٠﴾ فَجَعَلْنَٰهُ فِى قَرَارٍ مَّكِينٍ ﴿٢١﴾ إِلَىٰ قَدَرٍ
مَّعْلُومٍ ﴿٢٢﴾ فَقَدَرْنَا فَنِعْمَ ٱلْقَٰدِرُونَ ﴿٢٣﴾ وَيْلٌ يَوْمَئِذٍ لِّلْمُكَذِّبِينَ ﴿٢٤﴾
أَلَمْ نَجْعَلِ ٱلْأَرْضَ كِفَاتًا ﴿٢٥﴾ أَحْيَآءً وَأَمْوَٰتًا ﴿٢٦﴾ وَجَعَلْنَا فِيهَا رَوَٰسِىَ
شَٰمِخَٰتٍ وَأَسْقَيْنَٰكُم مَّآءً فُرَاتًا ﴿٢٧﴾ وَيْلٌ يَوْمَئِذٍ لِّلْمُكَذِّبِينَ ﴿٢٨﴾
ٱنطَلِقُوٓا۟ إِلَىٰ مَا كُنتُم بِهِۦ تُكَذِّبُونَ ﴿٢٩﴾ ٱنطَلِقُوٓا۟ إِلَىٰ ظِلٍّ ذِى ثَلَٰثِ
شُعَبٍ ﴿٣٠﴾ لَّا ظَلِيلٍ وَلَا يُغْنِى مِنَ ٱللَّهَبِ ﴿٣١﴾ إِنَّهَا تَرْمِى بِشَرَرٍ
كَٱلْقَصْرِ ﴿٣٢﴾ كَأَنَّهُۥ جِمَٰلَتٌ صُفْرٌ ﴿٣٣﴾ وَيْلٌ يَوْمَئِذٍ لِّلْمُكَذِّبِينَ ﴿٣٤﴾
هَٰذَا يَوْمُ لَا يَنطِقُونَ ﴿٣٥﴾ وَلَا يُؤْذَنُ لَهُمْ فَيَعْتَذِرُونَ ﴿٣٦﴾ وَيْلٌ يَوْمَئِذٍ
لِّلْمُكَذِّبِينَ ﴿٣٧﴾ هَٰذَا يَوْمُ ٱلْفَصْلِ جَمَعْنَٰكُمْ وَٱلْأَوَّلِينَ ﴿٣٨﴾ فَإِن كَانَ
لَكُمْ كَيْدٌ فَكِيدُونِ ﴿٣٩﴾ وَيْلٌ يَوْمَئِذٍ لِّلْمُكَذِّبِينَ ﴿٤٠﴾ إِنَّ ٱلْمُتَّقِينَ فِى
ظِلَٰلٍ وَعُيُونٍ ﴿٤١﴾ وَفَوَٰكِهَ مِمَّا يَشْتَهُونَ ﴿٤٢﴾ كُلُوا۟ وَٱشْرَبُوا۟ هَنِيٓـًٔا
بِمَا كُنتُمْ تَعْمَلُونَ ﴿٤٣﴾ إِنَّا كَذَٰلِكَ نَجْزِى ٱلْمُحْسِنِينَ ﴿٤٤﴾ وَيْلٌ يَوْمَئِذٍ
لِّلْمُكَذِّبِينَ ﴿٤٥﴾ كُلُوا۟ وَتَمَتَّعُوا۟ قَلِيلًا إِنَّكُم مُّجْرِمُونَ ﴿٤٦﴾ وَيْلٌ يَوْمَئِذٍ
لِّلْمُكَذِّبِينَ ﴿٤٧﴾ وَإِذَا قِيلَ لَهُمُ ٱرْكَعُوا۟ لَا يَرْكَعُونَ ﴿٤٨﴾ وَيْلٌ
يَوْمَئِذٍ لِّلْمُكَذِّبِينَ ﴿٤٩﴾ فَبِأَىِّ حَدِيثٍ بَعْدَهُۥ يُؤْمِنُونَ ﴿٥٠﴾

onyozeka (madzi a mbewu ya munthu)?

(21) Kenako tidawaika pamalo okhazikika (kuti chilengedwe chake chikwanire pamenepo).

(22) Mpaka nyengo yodziwika (imene tidaipima kuti mwana abadwe).

(23) Tidaipima nyengoyo; taonani kupima bwino Ife Opima!

20-23 [Kodi inu makafirinu sitidakulengeni kuchokera ku madzi wofooka, wonyozeka umene uli umuna? Ndipo tidawaika madzi amenewa pa malo wosungika bwino amene ali chiberekero cha mzimayi kufikira mu nthawi yopimidwa ndi yodziwika kwa Allah? Ndipo tidakonza bwino za kumulenga kwake ndi maonekedwe ake komanso kumutulutsa kwake. Taonani kukoma kwa opima nthawizo!]

(24) Kuonongeka kwakukulu tsiku limenelo kuli pa otsutsa (lonjezo Lathu ndi la kuuka kwa akufa). [Chionongeko komanso chilango choopsa Tsiku Lakiyama chili kwa okanira chilinganizo Chathu].

(25) Kodi sitidaichite nthaka kukhala yofungatira,

(26) Amoyo ndi akufa?

(27) Ndipo tidaika m'menemo mapiri ataliatali (oilimbitsa nthaka) ndipo takumwetsani madzi okoma.

25-27 [Kodi sitidaichite nthaka iyi yomwe mukukhalayi kukhala yofungatira pamwamba pake zamoyo zosawerengeka komanso m'kati mwake zakufa (za nkhaninkhani) zosawerengeka. Ndipo tidaika pamenepo mapiri olimbitsa (nthaka) okwera kuti nthakayo isatekeseke nanu, ndipo takumwetsani madzi okoma olowa bwino kum'mero?]

(28) Kuonongeka kwakukulu tsiku limenelo kuli pa otsutsa (lonjezo Lathu ndi la kuuka kwa akufa). [Chionongeko komanso chilango choopsa Tsiku Lakiyama chili kwa okanira chilinganizo Chathu].

(29) (kudzanenedwa kwa okana tsiku la chimaliziro): "Pitani ku zimene mudali kuzitsutsa zija".

(30) "Pitani ku mthunzi (wa utsi wa ku moto) wa nthambi zitatu,

(31) "Simthunzi (wamtendere) ndiponso siwotchinjiriza ku malawi a moto"

(32) Ndithu motowo umaponya mphalikira zazikuluzikulu ngati nyumba.

(33) Zonga ngati ngamira zachikasu.

29-33 [Tsiku Lakiyama kudzanenedwa kwa okanira kuti: "Pitani ku chilango cha jahena chomwe mudali kuchitsutsa chija pa dziko lapansi, pitani ndipo mukakhale pa mthunzi wa utsi wa jahena womwe wagawikana magawo atatu, mthunzi umenewo siungatchinjirize kutentha kwa tsiku limenelo komanso siungatsekereze ku malawi kena kalikonse. Ndithu jahena idzikaponya kuchokera ku moto mphalikira zikuluzikulu. Mphalikira iliyonse mwa zimenezo ngati nyumba zomangidwa kwambiri mukukula kwake ndi kutukuka. Mphalikira za jahena zimene zikauluka m'menemo zili ngati ngamira zakuda mtundu wake wom'kera ku chikasu].

(34) Kuonongeka kwakukulu tsiku limenelo kuli pa otsutsa (lonjezo Lathu ndi la kuuka kwa akufa). [Chionongeko komanso chilango choopsa Tsiku Lakiyama chili kwa okanira chilinganizo Chathu].

(35) Ili ndi tsiku lomwe sadzalankhula (chilichonse chothandiza).

(36) Ndipo sadzapatsidwa chilolezo (choyankhulira) kuti apereke madandaulo awo.

35-36 [Ili ndi Tsiku Lakiyama lomwe sadzayankhula m'menemo anthu okanira ndi mawu owathandiza ngakhalenso sadzapatsidwa iwowo chilolezo choti n'kuyankhula kuti adandaule ayi chifukwa choti alibe dandaulo lili lonse (lomveka).

(37) Kuonongeka kwakukulu tsiku limenelo kuli pa otsutsa (lonjezo Lathu ndi la kuuka kwa akufa). [Chionongeko komanso chilango choopsa Tsiku Lakiyama chili kwa okanira chilinganizo Chathu].

(38) (Adzauzidwa kuti): Ili ndi tsiku loweluza (pakati pa abwino ndi oipa), takusonkhanitsani inu (otsutsa Muhammad SAW) ndi (otsutsa aneneri) akale.

(39) Ngati muli ndi ndale yodzipulumutsira ku chilango Changa, ndichiteni ndaleyo.

38-39 [Ili ndi tsiku lomwe Allah agemule pakati pa zolengedwa ndipo choona chidziwika ku chabodza. Takusonkhanitsani lero inu makafiri a m'badwo uno ndi makafiri oyambirira mu mibadwo imene idapita. Ngati muli ndi ndale zodzipulumutsira ku chilango, ndiye chitani ndipo dziomboleni nokha ku chilango cha Allah ndi kubwezera Kwake.]

(40) Kuonongeka kwakukulu tsiku limenelo kuli pa otsutsa (lonjezo Lathu ndi la kuuka kwa akufa). [Chionongeko komanso chilango choopsa Tsiku Lakiyama chili kwa okanira chilinganizo Chathu].

(41) Ndithu oopa (Allah tsiku limenelo) adzakhala m'mithunzi ndi m'mitsinje.

(42) Ndipo adzakhala ndi zipatso zomwe azidzazifuna.

(43) (kudzanenedwa kwa iwo): "Idyani, imwani mokondwa chifukwa cha zabwino zomwe mudali kuchita (mu umoyo wa dziko lapansi).

(44) Ndithu, umo ndi m'mene Ife timawalipirira ochita zabwino.

(45) Kuonongeka kwakukulu tsiku limenelo kuli pa otsutsa (lonjezo Lathu ndi la kuuka kwa akufa).

41-45 [Ndithu anthu amene adaopa Mbuye wawo pa dziko lapansi naopa chilango Chake potsatira malamulo Ake ndi kupewa zoletsa Zake, iwowo Tsiku Lakiyama akakhala m'mithunzi ya mitengo yagubidi ndi mitsinje yoyenda ya madzi, ndi zipatso zambirimbiri mu zomwe mitima yawo izikazifuna ndi kusangalala nazo zikanenedwa kwa iwo: "Idyani kudya kokoma ndipo imwani kumwa kwabwino chifukwa cha zomwe mudatsogoza pa dziko lapansi. Ndithudi Ife mofanana ndi malipiro akulu amenewa timawalipirira anthu ochita zabwino mu ntchito zawo ndi kumvera kwawo. Chionongeko komanso chilango choopsa Tsiku Lakiyama chili kwa okanira tsiku la malipiro ndi chiwerengero cha ntchito za anthu ndi zomwe zili m'menemo mu mtendere ndi chilango].

(46) "Idyani sangalalani pang'ono m'kanthawi kochepa; ndithu inu ndinu ochimwa (chifukwa chakum'phatikiza Allah ndi zolengedwa).

[Kenako Allah awaopseza makafiri ndipo adati: "Idyani mu zokoma za dziko lapansi ndipo sangalalani ndi zilakolako zake zakuthazo, kanthawi kochepa, ndithudi ndinu oipa popembedza limodzi ndi Allah milungu ina yabodza].

(47) Kuonongeka kwakukulu tsiku limenelo kuli pa otsutsa (lonjezo Lathu ndi la kuuka kwa akufa). [Chionongeko komanso chilango choopsa Tsiku Lakiyama chili kwa okanira chilinganizo Chathu].

(48) Ndipo kukanenedwa kwa iwo kuti weramani (pembedzani Allah) sakuwerama

[Kukanenedwa kwa opembedza mafano amenewa kuti : "m'chitireni swalaat Allah ndipo dzichepetseni kwa Iye, sakudzichepetsa komanso sakupemphera koma akukakamira podzikweza kwawoko.]

(49) Kuonongeka kwakukulu tsiku limenelo kuli pa otsutsa (lonjezo Lathu ndi la kuuka kwa akufa).

(50) Kodi ndi nkhani iti imene adzaikhulupirira pambuyo pa iyi (Qur'aan).

49-50 [Kuonongeka ndi chilango choopsa Tsiku Lakiyama chikakhala cha okanira ma Ayah a Allah. Ngati simuikhulupirira Qur'aan imeneyi , kodi ndi buku liti komanso mawu ati pambuyo pake angakhulupirire? Kumachita Qur'aaniyi ndi yofotokozera bwino lomwe chinthu chilichonse, yonenetsa poyera ndi momveka bwino mu luntha lake malamulo ake ndi nkhani zake, yodabwitsa mu mawu ake komanso matanthauzo ake.]

## (78) SUURAT –UL-AN'NABAI

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Kodi akufunsana zachiyani (wina ndi mnzake)?

(2) Za nkhani yaikulu ija (yomwe ndi umodzi wa Allah, kupatulika kwa Qur'aan, utumiki wa Muhammad (SAW) ndi kudza kwa tsiku la kuuka kwa akufa)?

(3) Imene iwo akusiyana (ena akuikanira pomwe ena akuivomereza).

1-3 [Kodi ndi chinthu chanji makafiri a Maquraish akufunsana wina ndi mnzake? Akufunsana za nkhani yaikulu mu zochitika zake yomwe ndi Qur'aan Yaikulu imene ikufotokoza za kuuka kwa akufa komwe akukukaikira makafiri a Chiquraish ndi kukanira.]

(4) Aleke! Adzadziwa posachedwapa.

(5) Ayi, ndithu, (aleke zimenezo) posachedwapa adzadziwa zoona zake (pamene chilango chidzawatsikire).

ترتيبها ٧٨ — سُورَةُ النَّبَإِ — آياتها ٤٠

بِسْمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحْمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

عَمَّ يَتَسَآءَلُونَ ١ عَنِ ٱلنَّبَإِ ٱلْعَظِيمِ ٢ ٱلَّذِى هُمْ فِيهِ مُخْتَلِفُونَ ٣
كَلَّا سَيَعْلَمُونَ ٤ ثُمَّ كَلَّا سَيَعْلَمُونَ ٥ أَلَمْ نَجْعَلِ ٱلْأَرْضَ مِهَٰدًا ٦
وَٱلْجِبَالَ أَوْتَادًا ٧ وَخَلَقْنَٰكُمْ أَزْوَٰجًا ٨ وَجَعَلْنَا نَوْمَكُمْ سُبَاتًا
٩ وَجَعَلْنَا ٱلَّيْلَ لِبَاسًا ١٠ وَجَعَلْنَا ٱلنَّهَارَ مَعَاشًا ١١ وَبَنَيْنَا
فَوْقَكُمْ سَبْعًا شِدَادًا ١٢ وَجَعَلْنَا سِرَاجًا وَهَّاجًا ١٣ وَأَنزَلْنَا
مِنَ ٱلْمُعْصِرَٰتِ مَآءً ثَجَّاجًا ١٤ لِّنُخْرِجَ بِهِۦ حَبًّا وَنَبَاتًا ١٥ وَجَنَّٰتٍ
أَلْفَافًا ١٦ إِنَّ يَوْمَ ٱلْفَصْلِ كَانَ مِيقَٰتًا ١٧ يَوْمَ يُنفَخُ فِى ٱلصُّورِ
فَتَأْتُونَ أَفْوَاجًا ١٨ وَفُتِحَتِ ٱلسَّمَآءُ فَكَانَتْ أَبْوَٰبًا ١٩ وَسُيِّرَتِ
ٱلْجِبَالُ فَكَانَتْ سَرَابًا ٢٠ إِنَّ جَهَنَّمَ كَانَتْ مِرْصَادًا ٢١ لِّلطَّٰغِينَ
مَـَٔابًا ٢٢ لَّٰبِثِينَ فِيهَآ أَحْقَابًا ٢٣ لَّا يَذُوقُونَ فِيهَا بَرْدًا وَلَا شَرَابًا
٢٤ إِلَّا حَمِيمًا وَغَسَّاقًا ٢٥ جَزَآءً وِفَاقًا ٢٦ إِنَّهُمْ كَانُوا۟
لَا يَرْجُونَ حِسَابًا ٢٧ وَكَذَّبُوا۟ بِـَٔايَٰتِنَا كِذَّابًا ٢٨ وَكُلَّ شَىْءٍ
أَحْصَيْنَٰهُ كِتَٰبًا ٢٩ فَذُوقُوا۟ فَلَن نَّزِيدَكُمْ إِلَّا عَذَابًا ٣٠

4-5 [Zinthu sizili momwe akudzinamizira opembedza mafano amenewa. Adzadziwa opembedza mafano amenewa mapeto a kukanira kwawoko ndipo zidzaonekera kwa iwo zimene Allah adzawachite Tsiku Lakiyama, kenako zidzatsimikizika kwa iwo zimenezo ndipo kudzatsimikizika kwa iwo kuona kwa zomwe adabwera nazo Muhmmad (SAW) za Qur'aan ndi kuuka kwa akufa. Ichi ndi chiopsezo komanso lonjezo la mavuto kwa iwo.

6 Kodi sitidailenge nthaka kukhala ngati choyala? [Kodi sitidaichite nthaka kukhala yotambasuka ngati choyala?

7 Ndi mapiri ngati zichili zolimbika (nthaka)? [Ndi mapiri ngati zilimbikitso kuti nthaka isatekeseke nanu?

8 Ndipo tidakulengani mitundu iwiriiwiri. [Ndipo tidakulengani mitundumitundu achimuna ndi achikazi?

9 Ndipo tidachita tulo tanu kukhala mpumulo (ku mavuto a ntchito). [Ndipo tidachita tulo tanu kukhala mpumulo wa matupi anu , m'menemo mumapumuzika ndi kukhazikika].

10 Ndipo tidaupanga usiku kukhala ngati chovala (chanu pokuvundikirani ndi mdima wake). [Ndipo tidauchita usiku kukhala ngati chovala mdima wake umakuvekani ndi kumakuphimbani monga m'mene imamubisila nsalu munthu woivala].

11 Ndipo tapanga masana kukhala ngati nthawi yopezera zofunika pa moyo. [Ndipo tachita masana kukhala nthawi yoti inu muzifalikira (pa dziko) m'menemo kuti mudzipezere zosoweka za moyo wanu ndikuti muzigwira ntchito m'menemo mu zokukomerani.]

12 Ndipo tamanga pamwamba panu thambo zisanu ndi ziwiri zolimba.
[Ndipo tamanga pamwamba panu thambo zisanu ndi ziwiri zolimba kamangidwe kake, zolengedwa mwa luntha mopanda ming'alu kapena kuonongeka kulikonse].

13 Ndipo tidapanga nyali yowala ndi yotentha kwambiri (dzuwa). [Ndipo tidalichita dzuwa kukhala nyali yowala kwambiri].

14 Ndipo tawatsitsa madzi otsika mwamphamvu kuchokera ku mitambo ya mvula.

15 Kuti titulutse ndi madziwo mbewu ndi m'mera (chomwe ndi chakudya cha anthu ndi nyama).

16 Ndi minda yothonana nthambi za mitengo
14-16 [Ndipo tikuwatsitsa kuchokera ku mitambo ya mvula madzi wotsika mwamphamvu ndi mochuluka. Kuti titulutse ndi madzi amenewo nthangala zomwe anthu azidya ndi nsipu womwe nyama zimadya, komanso minda yothonana wina ndi unzake kuti nthambi zake zigawanikane.]

17 Ndithu, Tsiku la Chiweruzo ndi nthawi imene idakhazikitsidwa kale,

18 Tsiku limene lipenga lidzaimbidwa ndipo inu mudzabwera (ku bwalo losonkhanirana) muli m'magulumagulu.
17-18 [Ndithu tsiku lachilekanitso pakati pa zolengedwa lomwe ndi Tsiku la Kiyama lili nthawi ndi malo a lonjezo loikidwa kwa oyambirira komanso omalizira. Tsiku lomwe Mngero adzauzire mu lipenga chomwe ndi chidziwitso cha kuuka kwa akufa kotero inu muzidzabwera magulumagulu. M'badwo uliwonse limodzi ndi mtsogoleri wawo].

19 Ndipo thambo lidzatsegulidwa (mbali zonse) lidzakhala ndi makomomakomo.
[Ndipo thambo lidzatsekulidwa ndipo lidzakhala la makomo ambirimbiri otsikiramo angero].

20 Ndipo mapiri adzachotsedwa m'malo mwake, adzakhala ngati zideruderu.
[Ndipo mapiri adzayendetsedwa pambuyo poti adali olimba nakhala ngati zideruderu].

21 Ndithu, moto wa jahena ukuwadikilira (oipa).

22 Mbuto ya opyola malire.

إِنَّ لِلْمُتَّقِينَ مَفَازًا ﴿٣١﴾ حَدَآئِقَ وَأَعْنَٰبًا ﴿٣٢﴾ وَكَوَاعِبَ أَتْرَابًا ﴿٣٣﴾ وَكَأْسًا
دِهَاقًا ﴿٣٤﴾ لَّا يَسْمَعُونَ فِيهَا لَغْوًا وَلَا كِذَّٰبًا ﴿٣٥﴾ جَزَآءً مِّن رَّبِّكَ عَطَآءً
حِسَابًا ﴿٣٦﴾ رَّبِّ ٱلسَّمَٰوَٰتِ وَٱلْأَرْضِ وَمَا بَيْنَهُمَا ٱلرَّحْمَٰنِ لَا يَمْلِكُونَ
مِنْهُ خِطَابًا ﴿٣٧﴾ يَوْمَ يَقُومُ ٱلرُّوحُ وَٱلْمَلَٰٓئِكَةُ صَفًّا لَّا يَتَكَلَّمُونَ
إِلَّا مَنْ أَذِنَ لَهُ ٱلرَّحْمَٰنُ وَقَالَ صَوَابًا ﴿٣٨﴾ ذَٰلِكَ ٱلْيَوْمُ ٱلْحَقُّ فَمَن
شَآءَ ٱتَّخَذَ إِلَىٰ رَبِّهِۦ مَـَٔابًا ﴿٣٩﴾ إِنَّآ أَنذَرْنَٰكُمْ عَذَابًا قَرِيبًا يَوْمَ
يَنظُرُ ٱلْمَرْءُ مَا قَدَّمَتْ يَدَاهُ وَيَقُولُ ٱلْكَافِرُ يَٰلَيْتَنِى كُنتُ تُرَٰبًۢا ﴿٤٠﴾

## سُورَةُ ٱلنَّازِعَاتِ

ترتيبها ٧٩ — آياتها ٤٦

بِسْمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحْمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

وَٱلنَّٰزِعَٰتِ غَرْقًا ﴿١﴾ وَٱلنَّٰشِطَٰتِ نَشْطًا ﴿٢﴾ وَٱلسَّٰبِحَٰتِ سَبْحًا
﴿٣﴾ فَٱلسَّٰبِقَٰتِ سَبْقًا ﴿٤﴾ فَٱلْمُدَبِّرَٰتِ أَمْرًا ﴿٥﴾ يَوْمَ تَرْجُفُ ٱلرَّاجِفَةُ
﴿٦﴾ تَتْبَعُهَا ٱلرَّادِفَةُ ﴿٧﴾ قُلُوبٌ يَوْمَئِذٍ وَاجِفَةٌ ﴿٨﴾ أَبْصَٰرُهَا
خَٰشِعَةٌ ﴿٩﴾ يَقُولُونَ أَءِنَّا لَمَرْدُودُونَ فِى ٱلْحَافِرَةِ ﴿١٠﴾ أَءِذَا كُنَّا
عِظَٰمًا نَّخِرَةً ﴿١١﴾ قَالُوا۟ تِلْكَ إِذًا كَرَّةٌ خَاسِرَةٌ ﴿١٢﴾ فَإِنَّمَا هِىَ زَجْرَةٌ
وَٰحِدَةٌ ﴿١٣﴾ فَإِذَا هُم بِٱلسَّاهِرَةِ ﴿١٤﴾ هَلْ أَتَىٰكَ حَدِيثُ مُوسَىٰٓ ﴿١٥﴾

23 Adzakhala m'menemo muyaya.
24 Sadzalawa m'menemo kuzizira kapena chakumwa (chowachotsera ludzu).
25 Koma akalawa madzi wotentha kwambiri ndi mafinya (otuluka m'matupi a anthu a ku moto).
26 Adzalipidwa malipiro olingana ndi ntchito zawo.

21-25 [Ndithu jahena tsiku limenelo idzakhala ikuwayang'anitsitsa anthu okanira ndi kuwayembekezera amene udalinganizidwira chifukwa cha iwo. Malo obwerera a anthu okanira. Akakhala m'menemo zaka ndi zaka zotsatizana zosadukiza. Sakalakalaka m'menemo kupeza kuziziritsa kwa moto kwa iwo ngakhalenso chakumwa chowachotsera nacho ludzu ayi kupatula madzi ogaduka ndi mafinya a anthu a ku moto. Akalipidwa ndi zimenezo kukhala malipiro a chilungamo ofanana ndi ntchito zawo zimene adali n'kuzigwira pa dziko lapansi.]

27 Ndithu iwo sadali kuyembekezera chiwerengero (cha ntchito zawo kwa Allah).
28 Adatsutsa zizindikiro Zathu ndi mtsutso waukulu.
29 Ndipo chinthu chilichonse tachisunga molemba m'buku.
30 Basi, lawani (lero chilango Changa); sitikuwonjezerani chinthu china koma chilango pamwamba pa chilango,

27- 30 [Ndithu iwowo adali asakuopa tsiku la chiwerengero cha ntchito zawo ndipo sadaligwirire ntchito. Ndipo adakanira zomwe Atumiki adabweretsa kuzikanira kwenikweni. Chinthu chilichonse tinachidziwa ndi kuchilemba mu buku lalikulu lotchedwa Allahuhul Mahfuudhu. Choncho inu anthu okanira lawani malipiro a ntchito zanu ndipo sitidzakuonjezerani kena kake kupatula chilango pamwamba pa chilango chanu.]

31 Ndithu, kwa amene akuopa (Allah awakonzera) malo osonyeza kupambana.
32 Minda ndi zipatso za mphesa,
33 Ndi mabuthu a misinkhu yofanana,
34 Ndi zipanda zodzadza ndi zakumwa.
35 Sakamva m'menemo mawu opanda pake kapena bodza.

31- 35 [Ndithu anthu amene adaopa Mbuye wawo n'kumagwira nchito zolungama ali nako kupambana chifukwa cha kulowa kwawo ku jannah. Ndithu ali nayo minda ikuluikulu komanso mphesa. Ndipo akakhala nawo m'menemo akazi a misinkhu ing'onoing'ono, mabere oima mu msinkhu umodzi. Ndipo akakhala ndi zipanda zodzadza ndi mowa. Sakamva m'menemo kuyankhula kwa mawu achabe komanso sazikanamizana wina ndi mnzake.]

36 Amenewo ndi malipiro ochokera kwa Mbuye wako zopereka zokwanira).
37 Mbuye wa kumwamba ndi pansi ndi zimene zili pakati pake; Mwini chifundo chambiri. Palibe amene adzakhala ndi mphamvu yolankhula Naye (pa tsiku limenelo).
38 Tsiku limene adzaima jibril (AS) ndi angero pa mzere (ali odzichepetsa); sadzayankhula aliyense mwa iwo kupatula yekhayo amene adzaloledwa ndi Wachifundo chambiri ndipo adzanena zolondola.
39 Limenelo ndiye tsiku loona, lopanda chikaiko, choncho amene akufuna adzipezere malo (njira yonkera) kwa Mbuye wake.

36-39 [Adzakhala nazo zimenezo kukhala malipiro ndi chopereka chochokera kwa Allah ndi chopatsa chambiri chokwanira kwa iwo,Mbuye wa mitambo ndi nthaka ndi zomwe zili pakati pake. Iye ndi Wachifundo wa dziko lapansi komanso wa Tsiku Lomaliza. Yense sadzakhala ndi mphamvu zomufunsira kupatula

amene awalola kuti atero. Tsiku limene adzaima Jibril (AS) ndi angero ali mizeremizere ndipo sakadandaulira wina aliyense chikhulululuko kupatula amene adzamuloleze Wachifundo kutero ndipo adzanena zoona ndi zolungama. Limenelo ndilo tsiku loona lomwe lilibe chikaiko cha kuchitika kwake. Amene akufuna chipulumutso ku zoopsa zake adzichitire yekha kwa Mbuye wake malo obwerera pogwira ntchito zabwino.]

40 Ndithu, tikukuchenjezani za chilango chomwe chili pafupi kudza, tsiku limene munthu adzayang'ana zimene adatsogoza ndi manja ake, ndipo kafiri adzanena kuti: "Kalanga ine! Ndidakakhala dothi (kuti ndisalangidwe chilango chikundiyembekezerachi).

[Ndithu Ife takuchenjezani chilango cha Tsiku lomaliza lomwe layandikira. Tsiku limenelo adzaona munthu aliyense zimene adachita zabwino ndi zimene adachita zoipa ndipo kafiri adzalankhula chifukwa cha kuopsa kwa chiwerengero kuti: "Kalanga ine bola ndikadakhala dothi ndipo osaukitsidwa kwa akufa].

## (79) SUURAT - AN'NAAZI'AAT

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Ndikulumbirira (angero) amene amazula mizimu ya osakhulupirira mwamphamvu.

2 Ndikulumbiriranso angero amene amachotsa mizimu ya okhulupirira moleza.

3 Ndi omwe amasambira (nayo mizimuyo) mlengalenga (ponka nayo ku malo oyembekezera).

4 Ndi iwo amene akupikisana pokwaniritsa malamulo a Allah.

5 Ndi iwo amene akulongosola malamulo (Ake).

6 Pa tsiku lomwe (lipenga loyamba lidzaombedwa) dziko lapansi ndi mapiri zidzagwedezeka (ndipo aliyense adzafa).

7 Ndipo kudzatsatira kuomba kwa lipenga lachiwiri (kumene kudzaukitsa akufa onse).

1-7 [Allah Taalaa walumbirira angero amene amazula mizimu ya makafiri mwamphamvu komanso walumbirira angero amene amachotsa mizimu ya anthu okhulupirira mwapang'onopang'ono, moleza. Ndiponso walumbirira amene amasambira ndi potsika kuchokera kumwamba ndi pokwera pake. Kenako walumbirira angero amene amapikisana ndi kufulumizitsira popititsa malamulo a Allah. Kenakonso walumbirira angero amene amapititsa kuwachita malamulo a Mbuye wawo ku zomwe awapatsa udindo kuzikonza mu zinthu zoyendetsera dziko lapansi- ndipo nkosavomerezeka kwa zolengedwa kulumbirira wina wake wosakhala Mlengi wake, ndipo amene angatero ndiye kuti waphatikiza Allah ndi china chake pa ibaadah- Ndithudi zolengedwa zonse zidzaukitsidwa ndipo zidzawerengeredwa ntchito zake. Tsiku limene nthaka idzatekeseke pa nthawi ya kuimba lipemba loyamba kutekeseka kwakupha zonse, ndi kutsatira kuimba kwa lipenga kwina, koukitsa akufa kukhalanso amoyo.]

8 Mitima tsiku limenelo idzanjenjemera ndi kuopa.

9 Maso a eni mitimayo adzakhala ozyolika (chifukwa cha madandaulo).

8-9 [Mitima ya makafiri tsiku limenelo idzakhala yosakhazikika chifukwa cha mantha aakulu, maso a eni mitima imeneyo adzakhala oyaluka chifukwa cha kuopsa kwa zimene azidzaziona.]

10 (Osakhulupirira) akunena kuti: "Kodi n'zoona adzatibwezera pambuyo pa imfa monga tidalili kale?"

11 "Pomwe ife titakhala mafupa ofumbwa (tingadzabwezedwe ndi kuukitsidwa mwa tsopano?)

12 Adanena (mokanira ndi mwachipongwe): "Choncho kubwerera kumeneko ngati kudzakhalepodi kudzakhala kotaika.

10-12 [Akunena anthu amenewa okanirawa za kuuka kwa akufa kuti: "Kodi tingabwezeretsedwenso ife pambuyo pakufa kwathu kubwereranso m'mene tidalili pa dziko lapansi? Kodi tingabwezeretsedwe kumachita tidali mafupa ofumbwa? Akunena kuti: "Kubwerera kwathu kumeneko kudzakhala ngati zili dero kotaika, kwabodza."

13 (Musaganize kubwererako n'chinthu chovuta) Ndithundithu Kiyamayo ndi mkuwe umodzi.

14 Mwadzidzidzi (zolengedwa zonse) zidzangowona zili pa dziko latsopano (zili zamoyo).

13-14 [Ndithudi kudzangokhala kuuzira kamodzin'kamodzi, adzangozindikira ali amoyo pa mwamba pa dziko pambuyo poti adali m'kati mwake.]

15 Kodi yakufika( iwe Muhammad SAW) nkhani ya Mussa? [Kodi iwe Mtumiki (SAW) yakufika nkhani ya Mussa (AS)?

16 Pamene Mbuye wake adamuitana pa chigwa choyera (chotchedwa ) Tuwaa

17 (Adamuuza kuti): "Pita kwa Farawo ndithu iye wapyola malire.

18 Umuuze kuti: "kodi ukufuna kudziyeretsa?"

19 "Ndikuti ndikuongolere kwa Mbuye wako kuti (uzimuopa?"

إِذْ نَادَىٰهُ رَبُّهُۥ بِٱلْوَادِ ٱلْمُقَدَّسِ طُوًى ﴿١٦﴾ ٱذْهَبْ إِلَىٰ فِرْعَوْنَ إِنَّهُۥ طَغَىٰ ﴿١٧﴾
فَقُلْ هَل لَّكَ إِلَىٰٓ أَن تَزَكَّىٰ ﴿١٨﴾ وَأَهْدِيَكَ إِلَىٰ رَبِّكَ فَتَخْشَىٰ ﴿١٩﴾ فَأَرَىٰهُ
ٱلْءَايَةَ ٱلْكُبْرَىٰ ﴿٢٠﴾ فَكَذَّبَ وَعَصَىٰ ﴿٢١﴾ ثُمَّ أَدْبَرَ يَسْعَىٰ ﴿٢٢﴾ فَحَشَرَ
فَنَادَىٰ ﴿٢٣﴾ فَقَالَ أَنَا۠ رَبُّكُمُ ٱلْأَعْلَىٰ ﴿٢٤﴾ فَأَخَذَهُ ٱللَّهُ نَكَالَ ٱلْءَاخِرَةِ وَٱلْأُولَىٰٓ
﴿٢٥﴾ إِنَّ فِى ذَٰلِكَ لَعِبْرَةً لِّمَن يَخْشَىٰٓ ﴿٢٦﴾ ءَأَنتُمْ أَشَدُّ خَلْقًا أَمِ ٱلسَّمَآءُ بَنَىٰهَا
﴿٢٧﴾ رَفَعَ سَمْكَهَا فَسَوَّىٰهَا ﴿٢٨﴾ وَأَغْطَشَ لَيْلَهَا وَأَخْرَجَ ضُحَىٰهَا ﴿٢٩﴾
وَٱلْأَرْضَ بَعْدَ ذَٰلِكَ دَحَىٰهَآ ﴿٣٠﴾ أَخْرَجَ مِنْهَا مَآءَهَا وَمَرْعَىٰهَا ﴿٣١﴾
وَٱلْجِبَالَ أَرْسَىٰهَا ﴿٣٢﴾ مَتَٰعًا لَّكُمْ وَلِأَنْعَٰمِكُمْ ﴿٣٣﴾ فَإِذَا جَآءَتِ ٱلطَّآمَّةُ
ٱلْكُبْرَىٰ ﴿٣٤﴾ يَوْمَ يَتَذَكَّرُ ٱلْإِنسَٰنُ مَا سَعَىٰ ﴿٣٥﴾ وَبُرِّزَتِ ٱلْجَحِيمُ
لِمَن يَرَىٰ ﴿٣٦﴾ فَأَمَّا مَن طَغَىٰ ﴿٣٧﴾ وَءَاثَرَ ٱلْحَيَوٰةَ ٱلدُّنْيَا ﴿٣٨﴾ فَإِنَّ ٱلْجَحِيمَ
هِىَ ٱلْمَأْوَىٰ ﴿٣٩﴾ وَأَمَّا مَنْ خَافَ مَقَامَ رَبِّهِۦ وَنَهَى ٱلنَّفْسَ عَنِ ٱلْهَوَىٰ
﴿٤٠﴾ فَإِنَّ ٱلْجَنَّةَ هِىَ ٱلْمَأْوَىٰ ﴿٤١﴾ يَسْـَٔلُونَكَ عَنِ ٱلسَّاعَةِ أَيَّانَ مُرْسَىٰهَا
﴿٤٢﴾ فِيمَ أَنتَ مِن ذِكْرَىٰهَآ ﴿٤٣﴾ إِلَىٰ رَبِّكَ مُنتَهَىٰهَآ ﴿٤٤﴾ إِنَّمَآ أَنتَ مُنذِرُ
مَن يَخْشَىٰهَا ﴿٤٥﴾ كَأَنَّهُمْ يَوْمَ يَرَوْنَهَا لَمْ يَلْبَثُوٓا۟ إِلَّا عَشِيَّةً أَوْ ضُحَىٰهَا ﴿٤٦﴾

ترتيبها ٨٠ — سُورَةُ عَبَسَ — آياتها ٤٢

16-19 [Pa nthawi imene adamuitana Mussa (AS) Mbuye wake pa chigwa choyeretsedwa chamwayi chotchedwa Tuwaa ndipo adati kwa iye: "Pita kwa Farawo ndithudi iyeyo wapyola malire ponyoza ndipo ukamuuze iyeyo kuti: 'Kodi ukufuna kuti uwuyeretse mtima wako ku zinthu zoipa ndikuti uwukongoletse ndi chikhulupiriro ndikutinso ndikuwongolere ku kumumvera Mbuye wako, nkumamuopa?"

(20) (Basi Mussa AS) adamuonetsa (Farawo) chozizwitsa chachikulu.

(21) Koma (Farawo) adatsutsa (Mussa AS pa zimene adadza nazo zija) ndi kum'nyoza.

(22) Kenako adabwerera uku akulimbika kutsutsana Naye (Allah).

20-22 [Ndipo Mussa (AS) adamuonetsa Farawo chizindikiro chachikulu chomwe ndi ndodo ndi dzanja, koma Farawo adam'kana Mtumiki wa Allah Mussa (AS) ndipo adanyoza Mbuye wake kenako adatembenuka kusiya chikhulupiriro akuchitira khama pomutsutsa ndi kumupinga Mussa (AS).]

(23) Adasonkhanitsa afiti uku akuitana anthu.

(24) Nanena: "Ine ndine mbuye wanu wapamwambamwamba!"

(25) Pamenepo Allah adamulanga chifukwa cha mawu ake omalizira ndi oyamba.

(26) Ndithu, pa zimenezi pali phunziro (lalikulu) kwa yemwe akuopa Allah.

23-26 [Ndipo adasonkhanitsa anthu a mu ufumu wake nawaitana nanena kuti: "Ine ndine mbuye wanu amene palibenso mbuye wina pamwamba pake". Allah ndiye adamubwezera pomulanga ndi chilango pa dziko lapansi komanso Tsiku Lomaliza ndipo adamuchita kukhala phunziro ndi chilango kwa ena onga iye mwa anthu opandukira. Ndithu Farawo komanso zimene zidam'peza za chilango ndi phunziro kwa amene akuganizira mozama ndikutengera phunziro kusiya zolakwa.]

(27) Kodi kulengedwa kwanu (inu osakhulupirira za kuuka kwa akufa) n'kovuta kapena thambo limene adalimanga (posonkhanitsa mbali zake zonse zosiyanasiyana ndikukhala chinthu chimodzi)?

(28) Adatukula msinkhu wake ndikulikonza bwino (popanda pena pong'ambika kapena posiyana ndi pena).

(29) Amavindikira mdima mu usiku wake ndipo amatulutsa kuwala mu usana wake.

(30) Ndipo pambuyo pa zimenezo, nthaka adaiyala (kuti ikhale yoyenera kuikhala).

(31) Adatulutsa m'menemo madzi ake (potulutsa akasupe ndi kuyendetsa mitsinje) ndiponso nsipu wake (kuti nyama zizidya msipuwo).

(32) Ndipo mapiri adawakhazikitsa ndikuwalimbika).

(33) (Adachita zonse izi) chifukwa chokusangalatsani inu ndi ziweto zanu.

27-33 [Kodi kukuwukitsani kwa akufa inu anthu nkovuta mukuganizira kwanu kapena kulenga kwa thambo? Adalitukula pamwamba panu ngati chomanga, ndipo adatalikitsa msinkhu wake mu mlengalenga popanda posiyana kapena kuonongeka. Ndipo wadetsa usiku wake ndi kulowa kwa dzuwa lake, ndipo wautulutsa usana wake ndi kutuluka kwake kwa dzuwa. Ndipo nthaka pambuyo polenga thambo, waitambasula ndipo adaika m'menemo zothandiza zake. Komanso adatulutsa akasupe a madzi ndipo adameretsa pamenepo zomwe zingamadyebwe mu zomera. Ndipo adalimbikitsa m'menemo mapiri kukhala zichili zake. Allah Subhaanahu adalenga mitendere yonseyi kukhala zithandizo zanu ndi ziweto zanu. (Ndithu kubwezeretsa zolengedwa Tsiku Lakiyama nkofewa kwa Allah kuposa kuzilenga zinthu zonsezi. Zonsezo kwa Allah n'zofewa, zosavuta).]

(34) Choncho likadzafika tsoka lalikulu (Tsiku la Kiyama).

35 Tsiku limenelo munthu adzakumbukira zimene adachita (zabwino kapena zoipa).
36 Ndipo moto waukali udzasonyezedwa kwa yense openya.
34-36 [Ikadzabwera Kiyama yaikulu ndi mavuto aakulu kumeneko ndiko kuwuzira kwachiwiri, nthawi imeneyo adzaonetsedwa munthu ntchito zake zonse mu zabwino ndi zoipa zomwe ndiye adzazikumbukira ndi kuzivomereza. Ndipo jahena idzaonetsedwa kwa aliyense woyang'ana, ikawonedwa ndi maso poyera.]
37 Tsono amene adapyola malire (mmachimo ake),
38 Ndipo ndikudzisankhira (yekha) umoyo wa pa dziko lapansi,
39 Ndithu, jahena ndiwo malo ake (palibe kwina).
37-39 [Tsono amene adapandukira malamulo a Allah, nadzisankhira umoyo wa dziko lapansi kuposa umoyo wa Tsiku Lomaliza ndithu mapeto ake ndi ku moto]
40 Tsono amene akuopa kuti adzaimirira pa maso pa Mbuye wake, nauletsa mtima wake ku zilakolako zoipa,
41 Ndithu, munda wa mtendere ndiwo adzakhale malo ake.
40-41 [Tsono amene akuopa kukaima pa maso pa Allah kukawerengeredwa ntchito zimene ankachita, ndi kuwuletsa mtima zilakolako zoipitsa, ndithudi jannah ndiwo malo ake.
42 Akukufunsa (iwe Muhammad SAW) za nthawi (ya Tsiku Lomaliza ): "Idzakhala liti?"
43 Uli ndi mphamvu yanji iwe yofotokozera Tsiku a Kiyamalo? (Iwe ulibe kuzindikira za nthawiyo kotero kuti ungaitchule kwa iwo).
44 Mbuye wako ndi Amene ali ndi kuzindikira kudza kwake.
45 Iwe (ntchito yako) ndi kuwachenjeza amene akuiopa; osati kulengeza za nthawi yake).
46 Tsiku limene adzaiona adzakhala ngati sadakhale (pa dziko lapansi nthawi yaitali) koma ngati madzulo amodzi kapena masana ake.
42-46 [Akukufunsa anthu opembedza mafanowa mopeputsa iwe Mtumiki (SAW) za nthawi yokwanira kuchitika kwa Kiyama yomwe ukuwalonjeza nayo. Iwe siuli pakalikonse ka kuzindikira za kiyamayo, koma kobwezeretsa zimenezo ndi kwa Allah Amene ali wopambana komanso Woyenera. Ndithu zinthu zimene zikukhudza iwe (SAW) zokhudzana ndi Kiyama, ndiko kuti uwachenjeze za imeneyo kwa amene akuiopa. Tsiku limene adzaione kuchitika kwa Kiyamayo, adzaona ngati kuti iwo sadakhale mu umoyo wa dziko lapansi chifukwa cha mavuto a Kiyama kupatula ngati nyengo ya pakati pa Zuhr ndi kulowa kwa dzuwa kapena pakati pa kutuluka kwa dzuwa mpaka theka la usana.]

# (80) SUURAT 'ABASA

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Adachita tsinya (Mneneri (SAW) ndi kuyang'ana kumbali.
2 Chifukwa chakuti adam'dzera wakhungu (kudzam'funsa zokhudzana ndi chipembedzo chake pamene iye adali kuyankhula ndi atsogoleri a Chiquraish).
1-2 [ kudawoneka kusintha ndi tsinya pa nkhope ya Mtumiki (SAW) ndipo adayang'ana kumbali chifukwa cha munthu wakhungu Abdullah Bin Ummi Maktum (RA) amene adamufikira kuti apeze chiongoko. Ndipo Mtumiki (SAW) adali atatanganidwa ndi kuitanira akuluakulu a Chiquraish ku Chisilamu.]
3 Nanga ungadziwe bwanji kuti mwina iye angadziyeretse (pomvera ulaliki wako watsopano)?
4 Kapena akumbukira, ndipo kukumbukirako kum'thandiza?
3-4 [Ndi chinthu chanji chikuchititse kudziwa zoona zake za munthuyo? Mwina ndi kufunsa kwake mtima wake uyera kapena kupezeka kwa iye kuonjezera kuganizira ndi kuleka zoipa.]
5 Koma amene wadzikwaniritsa (ndi chuma chake ndi mphamvu zake)
6 Ameneyo ndi yemwe ukumuchitira chidwi.
7 Palibe chilichonse pa iwe ngati sadziyeretsa.
5-7 [Tsono amene wadzikwaniritsa kuti sangasowe chiongolo chako, ndiye iwe ukumuchitira chidwi iyeyo ndipo ukumvera mawu ake. Pali chinthu chanji pa iwe akapanda kudziyeretsa ku ukafiri wake?"]
8 Koma amene wakudzera uku akuthamanga (kufuna maphunziro ndi chiongoko),
9 Ndipo iye akuopa (Allah mu mtima mwake)
10 Za iye, iwe sukusamala (ukuikira chidwi kwa wina).
11 Sichoncho! Ndithudi iyi (Qur'aan) ndi chikumbutso (chenjezo).
12 Basi, amene wafuna alangizika (ndi Qur'aan ndipo amene sakufuna m'siye).
13 (Malangizowa akuchokera) m'makalata olemekezeka (kwa Allah).
14 Apamwamba ndiponso oyeretsedwa (ku mbiri iliyonse yipunguka)
15 Omwe ali m'manja mwa (angero amene Allah wawachita kukhala) alembi (Ake).
16 Olemekezeka, omvera.
8-16 [Tsono munthu amene ali ndi khama lokumana nawe, uku akuopa Allah kuti asapunguze mu chiongoko, ndiye iwe za iye siukulabadira. Zinthu osati m'mene

wachitiramu iwe Mtumiki (SAW), ndithu suurah imeneyi ndi ulaliki kwa iwe ndi kwa amene wakonda kuti alangiizike. Amene wafuna kukumbukira Allah ndi kutsogoleredwa ndi chivumbulutso Chake. Chivumbulutso ichi, chimene ndi Qur'aan chili m'makalata okulitsidwa, olemekezeka , apamwamba kalinganizidwe kake, oyeretsedwa ku uve ndi kuonjezera komanso kupunguka, ali m'manja mwa angero olemba, amene ali atumiki a Allah pakati Pake ndi zolengedwa Zake, olemekezeka kalengedwe, khalidwe lawo ndi zochita zawo ndi zabwino, zoyera.]

17 Waonongedwa (watembereredwa) munthu. N'kwanji kusayamika kwake kotereku!

18 Kuchokera m'chinthu chanji chimene iye adamulenga?

19 Kuchokera ku madzi (opanda pake) adamulenga, nakonzeratu m'kalengedwe kosiyanasiyana.

20 Kenako adam'fewetsera njira (yotulukira m'mimba mwa mayi wake).

21 Ndipo amam'chititsa kuti amwalire, namukumbura m'manda.

22 Kenako akadzafuna adzamuukitsa (pambuyo pa imfa).

23 Ayi ndithu sanakwaniritsebe (munthu) zimene adamulamula Mbuye wake (Allah chingakhale wakhala nthawi yaitali pa dziko lapansi).

17-23 [Watembereredwa munthu wokanira ndipo walangidwa,n'chiyani cham'chititsa kukanira kwambiri Mbuye wake! Kodi sadaone mu chinthu chanji Allah adamulenga iyeyo nthawi yoyambirira? Adamulenga kuchokera ku madzi ochepa – umene uli umuna- namulinganiza zigawozigawo kenako namufotokozera njira ya chabwino ndi choipa. Kenako amam'patsa imfa ndikumuchitira malo omukumbura m'manda. Kenako akadzafuna (Allah) Subhaanahu adzamupatsanso moyo ndi kumuukitsa pambuyo pa kufa kwake kuti akawerengedwe ntchito zake ndi kupeza malipiro. Zinthu sizili monga akunenera kafiri ndi m'mene akuchitira, ayi, ndipo iye sadachite zomwe Allah adamulamula kuzichita mu chikhulupiriro ndi kugwiritsa ntchito zomumvera Iye.]

24 Alingalire munthu (m'mene chilili) chakudya chake;

25 Ndithu Ife timagwetsa mvula yambiri (kuchokera ku mitambo),

26 Kenako timaing'amba nthaka kuti (mmera utuluke);

27 Timameretsa m'menemo njere (ya chakudya cha anthu ndi zina zimene amasunga ku nkhokwe).

28 Ndi mphesa ndi msipu.

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَٰنِ الرَّحِيمِ
عَبَسَ وَتَوَلَّىٰٓ ﴿١﴾ أَن جَآءَهُ ٱلْأَعْمَىٰ ﴿٢﴾ وَمَا يُدْرِيكَ لَعَلَّهُۥ يَزَّكَّىٰٓ ﴿٣﴾ أَوْ
يَذَّكَّرُ فَتَنفَعَهُ ٱلذِّكْرَىٰٓ ﴿٤﴾ أَمَّا مَنِ ٱسْتَغْنَىٰ ﴿٥﴾ فَأَنتَ لَهُۥ تَصَدَّىٰ ﴿٦﴾
وَمَا عَلَيْكَ أَلَّا يَزَّكَّىٰ ﴿٧﴾ وَأَمَّا مَن جَآءَكَ يَسْعَىٰ ﴿٨﴾ وَهُوَ يَخْشَىٰ ﴿٩﴾ فَأَنتَ
عَنْهُ تَلَهَّىٰ ﴿١٠﴾ كَلَّآ إِنَّهَا تَذْكِرَةٌ ﴿١١﴾ فَمَن شَآءَ ذَكَرَهُۥ ﴿١٢﴾ فِى صُحُفٍ مُّكَرَّمَةٍ
﴿١٣﴾ مَّرْفُوعَةٍ مُّطَهَّرَةٍۭ ﴿١٤﴾ بِأَيْدِى سَفَرَةٍ ﴿١٥﴾ كِرَامٍۭ بَرَرَةٍ ﴿١٦﴾ قُتِلَ ٱلْإِنسَٰنُ
مَآ أَكْفَرَهُۥ ﴿١٧﴾ مِنْ أَىِّ شَىْءٍ خَلَقَهُۥ ﴿١٨﴾ مِن نُّطْفَةٍ خَلَقَهُۥ فَقَدَّرَهُۥ ﴿١٩﴾ ثُمَّ
ٱلسَّبِيلَ يَسَّرَهُۥ ﴿٢٠﴾ ثُمَّ أَمَاتَهُۥ فَأَقْبَرَهُۥ ﴿٢١﴾ ثُمَّ إِذَا شَآءَ أَنشَرَهُۥ ﴿٢٢﴾ كَلَّا لَمَّا
يَقْضِ مَآ أَمَرَهُۥ ﴿٢٣﴾ فَلْيَنظُرِ ٱلْإِنسَٰنُ إِلَىٰ طَعَامِهِۦٓ ﴿٢٤﴾ أَنَّا صَبَبْنَا ٱلْمَآءَ صَبًّا
﴿٢٥﴾ ثُمَّ شَقَقْنَا ٱلْأَرْضَ شَقًّا ﴿٢٦﴾ فَأَنۢبَتْنَا فِيهَا حَبًّا ﴿٢٧﴾ وَعِنَبًا وَقَضْبًا ﴿٢٨﴾
وَزَيْتُونًا وَنَخْلًا ﴿٢٩﴾ وَحَدَآئِقَ غُلْبًا ﴿٣٠﴾ وَفَٰكِهَةً وَأَبًّا ﴿٣١﴾ مَّتَٰعًا لَّكُمْ
وَلِأَنْعَٰمِكُمْ ﴿٣٢﴾ فَإِذَا جَآءَتِ ٱلصَّآخَّةُ ﴿٣٣﴾ يَوْمَ يَفِرُّ ٱلْمَرْءُ مِنْ أَخِيهِ ﴿٣٤﴾
وَأُمِّهِۦ وَأَبِيهِ ﴿٣٥﴾ وَصَٰحِبَتِهِۦ وَبَنِيهِ ﴿٣٦﴾ لِكُلِّ ٱمْرِئٍ مِّنْهُمْ يَوْمَئِذٍ شَأْنٌ
يُغْنِيهِ ﴿٣٧﴾ وُجُوهٌ يَوْمَئِذٍ مُّسْفِرَةٌ ﴿٣٨﴾ ضَاحِكَةٌ مُّسْتَبْشِرَةٌ ﴿٣٩﴾ وَوُجُوهٌ
يَوْمَئِذٍ عَلَيْهَا غَبَرَةٌ ﴿٤٠﴾ تَرْهَقُهَا قَتَرَةٌ ﴿٤١﴾ أُو۟لَٰٓئِكَ هُمُ ٱلْكَفَرَةُ ٱلْفَجَرَةُ ﴿٤٢﴾

29 Ndi mzitona (wabwino) ndi (zipatso za) kanjedza.

30 Ndi minda yothothana nthambi za mitengo,

31 Ndi zipatso zodyedwa (ndi anthu) ndi msipu wodyedwa (ndi nyama).

32 Tazimeretsa zimenezo kuti zikondweretse inu ndi ziweto zanu.

24-32 [Choncho aganizire munthu m'mene Allah adalengera chakudya chake chomwe ndi chirimbikitso cha moyo wake? Ndithudi Ife tatsitsa madzi pa nthaka mwamphamvu kenako taing'amba nthakayo ndi zomwe tatulutsa kuchokera m'menemo mu zomera zosiyanasiyana. Ndipo tidameretsa m'menemo mbewu (njere), mphesa, msipu wa ziweto, mzitona,kanjedza ndi minda ya mitengo ikuluikulu komanso zipatso ndi msipu zomwe mukusangalala nazo inuyo ndi ziweto zanu.]

33 Ndipo likadzafika lipenga logonthetsa mkhutu ndi kuumitsa makosi,

34 Pa tsikuli munthu adzathawa m'bale wake,

35 Mayi wake ndi bambo wake,

36 Mkazi wake ndi ana ake.

37 Munthu aliyense mwa iwo, tsiku limenelo adzakhala ndi zakezake zotangwanika nazo (sadzalabadira za anzake).

آياتها ٢٩ — سُورَةُ التَّكۡوِيرِ — ترتيبها ٨١

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

إِذَا ٱلشَّمۡسُ كُوِّرَتۡ ١ وَإِذَا ٱلنُّجُومُ ٱنكَدَرَتۡ ٢ وَإِذَا ٱلۡجِبَالُ
سُيِّرَتۡ ٣ وَإِذَا ٱلۡعِشَارُ عُطِّلَتۡ ٤ وَإِذَا ٱلۡوُحُوشُ حُشِرَتۡ
٥ وَإِذَا ٱلۡبِحَارُ سُجِّرَتۡ ٦ وَإِذَا ٱلنُّفُوسُ زُوِّجَتۡ ٧ وَإِذَا
ٱلۡمَوۡءُۥدَةُ سُئِلَتۡ ٨ بِأَيِّ ذَنۢبٖ قُتِلَتۡ ٩ وَإِذَا ٱلصُّحُفُ نُشِرَتۡ
١٠ وَإِذَا ٱلسَّمَآءُ كُشِطَتۡ ١١ وَإِذَا ٱلۡجَحِيمُ سُعِّرَتۡ ١٢ وَإِذَا ٱلۡجَنَّةُ
أُزۡلِفَتۡ ١٣ عَلِمَتۡ نَفۡسٞ مَّآ أَحۡضَرَتۡ ١٤ فَلَآ أُقۡسِمُ بِٱلۡخُنَّسِ ١٥
ٱلۡجَوَارِ ٱلۡكُنَّسِ ١٦ وَٱلَّيۡلِ إِذَا عَسۡعَسَ ١٧ وَٱلصُّبۡحِ إِذَا تَنَفَّسَ ١٨
إِنَّهُۥ لَقَوۡلُ رَسُولٖ كَرِيمٖ ١٩ ذِي قُوَّةٍ عِندَ ذِي ٱلۡعَرۡشِ مَكِينٖ ٢٠ مُّطَاعٖ
ثَمَّ أَمِينٖ ٢١ وَمَا صَاحِبُكُم بِمَجۡنُونٖ ٢٢ وَلَقَدۡ رَءَاهُ بِٱلۡأُفُقِ ٱلۡمُبِينِ
٢٣ وَمَا هُوَ عَلَى ٱلۡغَيۡبِ بِضَنِينٖ ٢٤ وَمَا هُوَ بِقَوۡلِ شَيۡطَٰنٖ رَّجِيمٖ ٢٥
فَأَيۡنَ تَذۡهَبُونَ ٢٦ إِنۡ هُوَ إِلَّا ذِكۡرٞ لِّلۡعَٰلَمِينَ ٢٧ لِمَن شَآءَ مِنكُمۡ أَن
يَسۡتَقِيمَ ٢٨ وَمَا تَشَآءُونَ إِلَّآ أَن يَشَآءَ ٱللَّهُ رَبُّ ٱلۡعَٰلَمِينَ ٢٩

آياتها ١٩ — سُورَةُ الانفِطَارِ — ترتيبها ٨٢

33-37 [Ukadzabwera mkuwe wa Tsiku la Kiyama womwe ndi kuopsa kwake adzagontha makutu, tsiku limene munthu adzathawe chifukwa cha kuopsa kwa tsiku limenelo m'bale wake, mayi wake, bambo wake, mkazi wake ndi ana ake. Aliyense mwa iwowo tsiku limenelo adzakhala nazo zinthu zomutangwanitsa ndi kumuletsa kutangwanika ndi za ena.]

(38) Tsiku limenelo nkhope zina zikawala;
(39) Zosekerera ndi zachimwemwe (chifukwa cha nkhani yabwino ya kumunda wamtendere).
(40) Ndipo nkhope zina tsiku limenelo zidzakhala zokutidwa ndi fumbi.
(41) Mdima udzazikuta.
(42) Awa adzakhala anthu osakhulupirira, oipa (olakwira Allah).

38 – 42 [Nkhope za anthu a mtendere ku tsiku limenelo zidzakhala zowala, zosangalala, zachimwemwe. Ndipo nkhope za anthu a ku jahena zidzakhala za mdima, zakuda, kuyaluka kutazikuta. Iwowo amene ali ndi mbiri zimenezi ndi anthu amene adakanira mtendere wa Allah nakanira ma Ayah Ake ndipo adazilowerera mosalabadira zinthu zoletsedwa Zake poipitsa ndi kudumpha malire.]

# (81) SUURAT -TAKWIIR

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Pamene dzuwa lidzakulungidwe (ndi kuchotsedwa kuwala kwake),
(2) Ndi pamene nyenyezi zidzathothoke (ndi kuchoka m'malo mwake),
(3) Ndi pamene mapiri (adzagwedezedwe) ndi kuyendetsedwa (kuchoka m'malo mwake).
(4) Ndi pamene ngamira zabere la miyezi khumi zidzasiidwe (zopanda oziyang'anira),
(5) Ndi pamene nyama za m'tchire zidzasonkhanitsidwe pamodzi (kuchokera m'malo osiyanasiyana chifukwa cha kuopsa kwa tsikulo),
(6) Ndi pamene Nyanja zidzayatsidwe moto,
(7) Ndi pamene mizimu idzalumikizidwe (ndi matupi awo),
(8) Ndi pamene mwana wamkazi yemwe adaikidwa m'manda wamoyo adzafunsidwe,
(9) Ndi tchimo lanji adaphedwera?
(10) Ndi pamene makalata (momwe mudzalembedwa zochita za aliyense) adzatambasulidwe (kuti awerengedwe)
(11) Ndi pamene thambo lidzayalulidwe (kuchoka m'malo mwake),
(12) Ndi pamene jahena idzayatsidwe mwamphamvu,
(13) Ndi pamene jannah idzayandikitsidwe,
(14) (zikadzachitika izi ndi pamene) mzimu uliwonse udzadziwa zimene wabweretsa (zabwino kapena zoipa)

1-14 [Pamene dzuwa lidzakulungidwe ndi kuchoka kuwala kwake, ndi pamene nyenyezi zidzamwazikane ndi kuchoka kuwala kwake, ndi pamene mapiri adzayendetsedwe kuchotsedwa pamwamba pa nthaka nkukhala fumbi louluzika, ndi pamene ngamira zabere zidzasiidwe osalabadiridwa, ndi pamene nyama za m'tchire zidzasonkhanitsidwe ndi kusakaniziridwa kuti Allah apereke chibwezerano kwa zina ndi zim'nzake, ndi pamene Nyanja zidzayatsidwe moto nkudzala ngakhale zili zazikuluzikulu zikuyaka, ndi pamene mizimu idzayanjanitsidwe ndi yofanana nayo ndi inzake, ndi pamene mwana wamkazi amene adakwiriridwa m'manda wamoyo adzafunsidwe funso lomukometsa ndi kumuiwalitsa mavuto oyikidwira m'manda wamoyo kuti: "Ndi tchimo lanji adaikidwira m'manda wamoyo". Ndi pamene makalata a ntchito adzaonetsedwe, ndi pamene thambo lidzazulidwe ndi kuchotsedwa m'malo mwake, ndi pamene moto udzayatsidwe ndi kusonkhetsedwa, ndi pamene jannah yomwe ndi nyumba ya mtendere idzayandikitsidwe kwa anthu ake oopa Allah, zikadzachitika zimenezi mzimu uliwonse udzatsimikiza ndipo udzapeza zomwe udatsogoza zabwino kapena zoipa.]

(15) Ndikulumbirira nyenyezi zimene zimabwerera masana ndi kutulukanso usiku.
(16) Zomwe zimayenda kenako nkubisika,
(17) Ndi usiku pamene ukulowa.
(18) Ndi m'mawa kukamacha.
(19) Ndithu, iyi (Qur'aan) ndi liwu la Mtumiki (Gabriel AS) wa Allah wolemekezeka (kwa Iye).
(20) Mwini mphamvu ndi mwini ulemerero kwa Mwini Mpando wa chifumu.
(21) Womveredwa kumeneko ndiponso wokhulupirika (pa chivumbulutso).

15-21 [Allah walumbirira nyenyezi zobisika kuwala kwake masana,zoyenda nkumabisika mu njira zake (zimene zimayendamo), komanso walumbirira usiku ukamabwera ndi mdima wake, ndi kum'mawa kukamaonekera kuwala kwake, ndithudi Qur'aan imeneyi ndi uthenga wofikitsidwa ndi mtumiki wolemekezeka amene ali Jibril (AS), mwini mphamvu zopititsa ndi kuchititsa kuti zimene walamulidwa zigwire ntchito, mwini malo a pamwamba kwa Allah, angero amamumvera, wopatsidwa udindo wa chivumbultso chimene amatsika nacho.]

(22) Ndipo m'bale wanu uyu siwamisala ayi.
(23) Ndithu, ndikulumbira kuti (iye Muhammad SAW) adamuona (Jibril) m'chizimezime (cha kum'mawa) chooneka bwino.
(24) (Muhammad SAW) sali mbombo wa chivumbulutso (koma amafikitsa zonse ndi kuziphunzitsa kwa anthu).
(25) (Chivumbulutso chomwe chavumbulutsidwachi kwa iye) si mawu a satana wothamangitsidwa m'chifundo cha Allah.

22-25[Muhammad (SAW) amene mukumudziwayo sali wamisala. Ndithudi Muhammad (SAW) adamuona Jibril (AS) amene amamubwerera ndi uthenga mu chizimezime chakum'mawa chachikulu. Ndipo iye (SAW) sikuti ndi mbombo pofikitsa chivumbulutso. Ndipo Qur'aan imeneyi siliwu la satana wothamangitsidwa ku chifundo cha Allah koma amenewa ndi mawu a Allah ndi chivumbulutso Chake.]

(26) Nanga mukupita kuti?
(27) Sichina iyi (Qur'aan) koma ndi chikumbutso kwa zolengedwa zonse.
(28) Kwa yemwe mwa inu akufuna kuyenda mu njira yowongoka.
(29) Ndipo simungafune chinthu mwa inu nokha pokhapokha atafuna Allah Mbuye wa zolengedwa zonse.

26-29 [Nanga kodi nzeru zanu zikupita nanu kuti pokanira Qur'aan pambuyo pa maumboni achimvekerewa? Qur'aaniyi sichina koma ulaliki wochokera kwa Allah kupita kwa anthu onse. Kwa amene wafuna mwa inu kuti

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ
إِذَا ٱلسَّمَآءُ ٱنفَطَرَتۡ ١ وَإِذَا ٱلۡكَوَاكِبُ ٱنتَثَرَتۡ ٢ وَإِذَا ٱلۡبِحَارُ
فُجِّرَتۡ ٣ وَإِذَا ٱلۡقُبُورُ بُعۡثِرَتۡ ٤ عَلِمَتۡ نَفۡسٞ مَّا قَدَّمَتۡ
وَأَخَّرَتۡ ٥ يَٰٓأَيُّهَا ٱلۡإِنسَٰنُ مَا غَرَّكَ بِرَبِّكَ ٱلۡكَرِيمِ ٦ ٱلَّذِي
خَلَقَكَ فَسَوَّىٰكَ فَعَدَلَكَ ٧ فِيٓ أَيِّ صُورَةٖ مَّا شَآءَ رَكَّبَكَ ٨
كَلَّا بَلۡ تُكَذِّبُونَ بِٱلدِّينِ ٩ وَإِنَّ عَلَيۡكُمۡ لَحَٰفِظِينَ ١٠ كِرَامٗا
كَٰتِبِينَ ١١ يَعۡلَمُونَ مَا تَفۡعَلُونَ ١٢ إِنَّ ٱلۡأَبۡرَارَ لَفِي نَعِيمٖ ١٣ وَإِنَّ
ٱلۡفُجَّارَ لَفِي جَحِيمٖ ١٤ يَصۡلَوۡنَهَا يَوۡمَ ٱلدِّينِ ١٥ وَمَا هُمۡ عَنۡهَا بِغَآئِبِينَ
١٦ وَمَآ أَدۡرَىٰكَ مَا يَوۡمُ ٱلدِّينِ ١٧ ثُمَّ مَآ أَدۡرَىٰكَ مَا يَوۡمُ ٱلدِّينِ
١٨ يَوۡمَ لَا تَمۡلِكُ نَفۡسٞ لِّنَفۡسٖ شَيۡـٔٗاۖ وَٱلۡأَمۡرُ يَوۡمَئِذٖ لِّلَّهِ ١٩

ترتيبها ٨٣ — سُورَةُ المُطَفِّفِينَ — آياتها ٣٦

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ
وَيۡلٞ لِّلۡمُطَفِّفِينَ ١ ٱلَّذِينَ إِذَا ٱكۡتَالُواْ عَلَى ٱلنَّاسِ يَسۡتَوۡفُونَ ٢
وَإِذَا كَالُوهُمۡ أَو وَّزَنُوهُمۡ يُخۡسِرُونَ ٣ أَلَا يَظُنُّ أُوْلَٰٓئِكَ أَنَّهُم
مَّبۡعُوثُونَ ٤ لِيَوۡمٍ عَظِيمٖ ٥ يَوۡمَ يَقُومُ ٱلنَّاسُ لِرَبِّ ٱلۡعَٰلَمِينَ ٦

alungame pa choonadi ndi chikhulupiriro, ndipo simungafune kulungamika ndiponso simungathe kutero pokhapokha ndi chifuniro cha Allah Mbuye wa zolengedwa zonse.]

## (82) SUURAT –UL- INFITWAAR

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Pamene thambo lidzasweke,
(2) Ndi pamene nyenyezi zidzayoyoke (ndi kumwazikana),
(3) Pamenenso nyanja zikuluzikulu zidzaphwasulidwe.
(4) Ndiponso pamene manda adzafukulidwe (ndi kutuluka akufa omwe adali m'menemo)
(5) (Pa nthawiyo) mzimu uliwonse udzadziwa zimene udatsogoza (zabwino ndi zoipa) ndi zimene udasiya m'mbuyo.

1-5 [Pamene thambo lidzang'ambidwe ndi kusokonekera chikhalidwe chake, ndiponso pamene nyenyezi zidzathothoke, ndi pamene nyanja Allah adzaziphwasule zina kulowa mu zimnzake ndi kuchoka madzi ake, ndi pamene manda adzatembenuzidwe potulutsa kunja zimene zidali m'menemo, pa nthawi imeneyo, mzimu uliwonse udzadziwa ntchito zake zonse

zomwe zidatsogolera kuchokera ku iyo ndi zomwe zidachedwa kuzichita ndi kulipidwa nazo.]

6 E, Iwe munthu! N'chiyani chakunyenga (kum'siya) Mbuye wako waufulu (kufikira ponyoza)?

7 Amene adalenga iwe nakulinganiza (ziwalo zako) ndi kukulongosola (moyenera).

8 Ndipo maonekedwe a mtundu uliwonse womwe adawafuna adakuveka (popanda chifuniro chako).

6-8 Ndi chiyani chakuchititsa kuti unyengeke ndi Mbuye wako Wopatsa, Wochulukitsa zabwino, Woyenerera kuthokozedwa ndi kumveredwa. Kodi Iye si Amene adakulenga iwe nalinganiza kalengedwe kako nakulongosola bwinobwino, ndipo adakuveka iwe, chifukwa choti ugwire ntchito zako, maonekedwe amene adawafuna Iye nkukulenga].

9 Ayi, sichoncho! Koma inu mukutsutsa za (tsiku) la malipiro.

10 Ndithu, inu alipo okuyang'anirani,

11 Olemekezeka, olemba zochitika zanu

12 Akudziwa (zonse) zimene mukuchita (zabwino ndi zoipa)

9-12 [Zinthu sizili momwe mukuneneramu mu zoti ndithu inu pa kupembedza kwanu zinthu zina zosakhala Allah kuti mukuyenerera, koma kuti mukulikanira tsiku la chiwerengero ndi malipiro. Ndipo ndithudi pa inu pali angero oyang'anira olemekezeka kwa Allah olemba zimene adapatsidwa udindo kuti azidzisunga. Palibe chimene chimadutsa mu nchito zanu ndi zinsinsi zanu kanthu kena kalikonse, amadziwa zonse inu mukuzichita zabwino kapena zoipa.]

13 Ndithudi, ochita zabwino adzakhala mu mtendere.

14 Ndipo ndithu, amene ali olakwira (malamulo a Allah) adzakhala ku moto wopsereza.

15 Adzaulowa tsiku la malipiro.

16 Ndipo iwo ku motoko sadzachokako.

13-16 [Ndipo ndithu anthu oipa amene adapeputsa mu zoyenera kuchitira Allah ndi zoyenera kuchitira akapolo Ake akakhala mu jahena, akawapeza malawi ake tsiku la malipiro. Ndipo iwo sikuti ku chilango cha jahena kuti akakhala kutali nacho ayi, osati potulukamo kapena imfa].

17 Kodi n'chiyani chakudziwitsa kuti tsiku la malipiro ndi chiyani?

18 Ndipo n'chiyani chakudziwitsa kuti tsiku la malipiro n'chiyani?

19 Limeneli ndi tsiku limene mzimu uliwonse siudzakhala ndi mphamvu (yodzetsa mtendere kapena yochotsa chovuta) pa mzimu wina. Ndipo lamulo pa tsiku limeneli ndi la Allah Yekha.

17-19 [Ndipo kodi ndi chiyani chikudziwitse iwe kuti kodi ukulu wa tsiku la chiwerengero ndi wotani? Kenakonso ndi chiyani chakudziwitsa kuti kodi ukulu wa tsiku la chiwerengero ndi wotani? Tsiku la chiwerengero sadzatha wina aliyense kuthandiza wina. Lamulo lonse pa tsiku limenelo ndi la Allah Yekha Amene palibe chopambana chimene chingamupambane. Ndipo palibe wogonjetsa chimene angamugonjetse, ndipo palibe angamusomphole Iye aliyense (ufumu Wake).]

# (83) SUURAT-UL-MUTAFFIFIINA

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Kuonongeka koopsa kukawapeza opunguza (miyezo ya malonda)

2 Iwo amene amati ena akamawayezera zinthu kwa anthu amafuna kulandira miyezo yodzadza.

3 Koma pamene iwo akugulitsa pa miyezo ya mbale kapena ya sikelo, amapungula (choyenera kulandira ogulawo).

4 Kodi amene (akupungula miyezo pa malondawo) sakuganiza kuti adzaukitsidwa,

5 Pa tsiku lalikulu (ndiponso loopsa)?

6 Tsiku limene adzaimirira anthu pa maso pa Mbuye wa zolengedwa.

1-6 [Chilango chowawitsa chikakhala cha anthu amene akupunguza anthu miyezo ya mbale ndi ya sikelo. Anthu omwe ngati akugula kuchokera kwa anthu ena zoyezedwa mu mbale kapena pa sikelo akumadzikwaniritsira eni akewo koma akamagulitsa anthu zoyezedwa ndi mbale kapena sikelo, amapunguza mu choyezeracho kapena sikeloyo. Kodi zikakhala bwanji kwa amene akumabera zinthu ziwiri zimenezi ndi kumapunguzira anthu zinthu zawo? Ndithu iyeyo ndi woyenerera kulandira chilango choopsa kuposa amene akupunguza miyezo ya mbale ndi sikelo. Kodi sakutsimikiza opunguza amenewa kuti ndithu Allah Taalaa adzawaukitsa kwa akufa ndi kuwawerengera ntchito zawo tsiku lalikulu mavuto ake? Tsiku limene adzaime anthu pa maso pa Allah ndi kudzawawerengera pa zazing'ono ndi zambiri. Ndipo iwowo mu zimenezo akakhala omvera kwa Allah Mbuye wa zolengedwa zonse.]

7 Ayi! Ndithu (siyani chinyengo pa malonda ndi kusalabadira za kuuka m'manda); zolembedwa za ntchito ya oipa zili mu sijjiini.

8 Nanga n'chiyani chitakudziwitse kuti sijjiini ndi chakutichakuti?

9 Ameneyu ndi kaundula wamkulu yemwe walembedwa (mkati mwake ntchito za anthu oipa).

7-9 [Zoonadi! Ndithu mapeto a anthu oipa ndi malo awo ndi othina. Kodi chitakudziwitse

كَلَّآ إِنَّ كِتَٰبَ ٱلۡفُجَّارِ لَفِي سِجِّينٖ ٧ وَمَآ أَدۡرَىٰكَ مَا سِجِّينٞ ٨ كِتَٰبٞ
مَّرۡقُومٞ ٩ وَيۡلٞ يَوۡمَئِذٖ لِّلۡمُكَذِّبِينَ ١٠ ٱلَّذِينَ يُكَذِّبُونَ بِيَوۡمِ ٱلدِّينِ ١١
وَمَا يُكَذِّبُ بِهِۦٓ إِلَّا كُلُّ مُعۡتَدٍ أَثِيمٍ ١٢ إِذَا تُتۡلَىٰ عَلَيۡهِ ءَايَٰتُنَا قَالَ أَسَٰطِيرُ
ٱلۡأَوَّلِينَ ١٣ كَلَّاۖ بَلۡۜ رَانَ عَلَىٰ قُلُوبِهِم مَّا كَانُواْ يَكۡسِبُونَ ١٤ كَلَّآ إِنَّهُمۡ
عَن رَّبِّهِمۡ يَوۡمَئِذٖ لَّمَحۡجُوبُونَ ١٥ ثُمَّ إِنَّهُمۡ لَصَالُواْ ٱلۡجَحِيمِ ١٦ ثُمَّ يُقَالُ
هَٰذَا ٱلَّذِي كُنتُم بِهِۦ تُكَذِّبُونَ ١٧ كَلَّآ إِنَّ كِتَٰبَ ٱلۡأَبۡرَارِ لَفِي عِلِّيِّينَ
١٨ وَمَآ أَدۡرَىٰكَ مَا عِلِّيُّونَ ١٩ كِتَٰبٞ مَّرۡقُومٞ ٢٠ يَشۡهَدُهُ ٱلۡمُقَرَّبُونَ
٢١ إِنَّ ٱلۡأَبۡرَارَ لَفِي نَعِيمٍ ٢٢ عَلَى ٱلۡأَرَآئِكِ يَنظُرُونَ ٢٣ تَعۡرِفُ فِي
وُجُوهِهِمۡ نَضۡرَةَ ٱلنَّعِيمِ ٢٤ يُسۡقَوۡنَ مِن رَّحِيقٖ مَّخۡتُومٍ ٢٥
خِتَٰمُهُۥ مِسۡكٞۚ وَفِي ذَٰلِكَ فَلۡيَتَنَافَسِ ٱلۡمُتَنَٰفِسُونَ ٢٦ وَمِزَاجُهُۥ
مِن تَسۡنِيمٍ ٢٧ عَيۡنٗا يَشۡرَبُ بِهَا ٱلۡمُقَرَّبُونَ ٢٨ إِنَّ ٱلَّذِينَ
أَجۡرَمُواْ كَانُواْ مِنَ ٱلَّذِينَ ءَامَنُواْ يَضۡحَكُونَ ٢٩ وَإِذَا مَرُّواْ بِهِمۡ
يَتَغَامَزُونَ ٣٠ وَإِذَا ٱنقَلَبُوٓاْ إِلَىٰٓ أَهۡلِهِمُ ٱنقَلَبُواْ فَكِهِينَ ٣١
وَإِذَا رَأَوۡهُمۡ قَالُوٓاْ إِنَّ هَٰٓؤُلَآءِ لَضَآلُّونَ ٣٢ وَمَآ أُرۡسِلُواْ عَلَيۡهِمۡ
حَٰفِظِينَ ٣٣ فَٱلۡيَوۡمَ ٱلَّذِينَ ءَامَنُواْ مِنَ ٱلۡكُفَّارِ يَضۡحَكُونَ ٣٤

kuti kuthina kumeneku nkotani? Imeneyo ndi ndende yamuyaya ndi chilango chopweteka, amenewo ndi amene adalembedwa kwa iwo kukhala mapeto awo. Adalembedwa ndipo kudatha palibe yowonjezera kapena kupungulidwa.]

10 Chilango chaukali tsiku limenelo chili kwa otsutsa.

11 Amene akutsutsa za tsiku la chiweruzo.

12 Ndipo palibe amene angalitsutse koma yekhayo opyola malire (pochita zoipa); wa machimo ambiri.

13 Pamene ma Ayah Athu akuwerengedwa kwa iye (onena za tsiku la malipiro ndi kuuka m'manda) amanena kuti: "Izi ndi nthano za anthu akale".

14 Iyayi, sichoncho! Koma yaphimbidwa mitima yawo ndi dzimbiri (la machimo) omwe akhala akukolola.

15 Zoona ndithu iwo amene (okanira tsiku limenelo) adzatchingidwa ku mtendere wa Mbuye wawo (sadzauona);

16 Pambuyo pake adzalowa ku moto (woyaka).

17 Kenako (adzauzidwa powaliritsa) "Ichi ndi chilango chomwe mudali kuchitsutsa (pa dziko lapansi)".

10-17 [Chilango choopsa tsiku limenelo chili kwa anthu okanira. Anthu amene amakanira kuchitika kwa tsiku la malipiro. Ndipo palibe amene angalikanire tsiku limenelo kupatula aliyense amene ali wopondereza, wochulukitsa machimo. Akamawerengedwa ma Ayah a Qur'aan amanena kuti: "Awa ndi mabodza a anthu oyambirira". Zinthu sikuti zili m'mene akudzinamizira, koma kuti amenewa ndi mawu a Allah ndi chivumbulutso Chake kwa Mtumiki Wake (SAW). Ndithudi mitima yawo idatchingidwa kuti sangaivomereze Qur'aaniyi ndi zomwe zaiphimba chifukwa chakuchuluka zimene amazichita mu zamachimo. Zinthu sizili monga m'mene akunenera anthu otsutsawa, koma ndithu iwowo Tsiku la Kiyama, za kuona Mbuye wawo, akatsekerezedwa. (Mu Ayah imeneyi muli maumboni osonyeza kuona anthu okhulupirira Mbuye wawo ku jannah). Ndithu iwo kenako akaulowa moto ndi kukamva kuotcha kwake. Zikanenedwa kwa iwo kuti: "Awa ndi malipiro a zomwe mudali kuzikanira].

18 Zoona, ndithu, kaundula wa anthu abwino (ochita ntchito zabwino) ali mu illiyyiina.

19 Nanga n'chiyani chitakudziwitse kuti illiyyuuna n'chakuti.

20 Ameneyu ndi kaundula wamkulu yemwe walembedwa (mkati mwake ntchito za anthu abwino);

21 Amaliikira umboni (angero) amene ayandikitsidwa (kwa Allah).

18-21 [Zoonadi ndithu buku la anthu abwino – amenewo ndiwo ali oopa Allah- ali m'masitepe a pamwamba ku jannah. Ndi chiyani chikudziwitse iwe Mtumiki (SAW) kuti masitepe a pamwambawa ndi chiyani? Limenelo ndi buku la anthu abwino lolelmbedwa ndipo kudatha kulembedwako palibe kuwonjezereka m'menemo kapena kupungulidwa. Amaliyang'ana limenelo amene ayandikitsidwa mwa angero a thambo lili lonse.]

22 Ndithu, ochita zabwino adzakhala mu mtendere,

23 Atakhala pa mipando yaulemu uku akuyang'ana (zimene Allah wawapatsa monga mtendere ndi ulemerero);

24 Udzadziwa kuwala kwa mtendere pa nkhope zawo.

25 Adzamwetsedwa vinyo (woyeretsedwa) ndi kutsekeredwa (ndi zitsekerero zolimba).

26 Komalizira kwake kwa vinyoyo (kudzatuluka fungo) la misk kuti akapeze zimenezi apikisane opikisana.

27 Ndipo chosakanizira (cha vinyoyo) ndi madzi a tasniim (ochokera ku jannah);

28 (Tasniimu ameneyo) ndi kasupe amene

عَلَى ٱلْأَرَآئِكِ يَنظُرُونَ ٣٥ هَلْ ثُوِّبَ ٱلْكُفَّارُ مَا كَانُوا۟ يَفْعَلُونَ ٣٦

## سُورَةُ الانشِقَاق
ترتيبها ٨٤ — آياتها ٢٥

بِسْمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحْمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

إِذَا ٱلسَّمَآءُ ٱنشَقَّتْ ١ وَأَذِنَتْ لِرَبِّهَا وَحُقَّتْ ٢ وَإِذَا ٱلْأَرْضُ مُدَّتْ
٣ وَأَلْقَتْ مَا فِيهَا وَتَخَلَّتْ ٤ وَأَذِنَتْ لِرَبِّهَا وَحُقَّتْ ٥ يَٰٓأَيُّهَا
ٱلْإِنسَٰنُ إِنَّكَ كَادِحٌ إِلَىٰ رَبِّكَ كَدْحًا فَمُلَٰقِيهِ ٦ فَأَمَّا مَنْ أُوتِىَ
كِتَٰبَهُۥ بِيَمِينِهِۦ ٧ فَسَوْفَ يُحَاسَبُ حِسَابًا يَسِيرًا ٨ وَيَنقَلِبُ
إِلَىٰٓ أَهْلِهِۦ مَسْرُورًا ٩ وَأَمَّا مَنْ أُوتِىَ كِتَٰبَهُۥ وَرَآءَ ظَهْرِهِۦ ١٠ فَسَوْفَ
يَدْعُوا۟ ثُبُورًا ١١ وَيَصْلَىٰ سَعِيرًا ١٢ إِنَّهُۥ كَانَ فِىٓ أَهْلِهِۦ مَسْرُورًا ١٣
إِنَّهُۥ ظَنَّ أَن لَّن يَحُورَ ١٤ بَلَىٰٓ إِنَّ رَبَّهُۥ كَانَ بِهِۦ بَصِيرًا ١٥ فَلَآ أُقْسِمُ
بِٱلشَّفَقِ ١٦ وَٱلَّيْلِ وَمَا وَسَقَ ١٧ وَٱلْقَمَرِ إِذَا ٱتَّسَقَ ١٨
لَتَرْكَبُنَّ طَبَقًا عَن طَبَقٍ ١٩ فَمَا لَهُمْ لَا يُؤْمِنُونَ ٢٠ وَإِذَا قُرِئَ
عَلَيْهِمُ ٱلْقُرْءَانُ لَا يَسْجُدُونَ ۩ ٢١ بَلِ ٱلَّذِينَ كَفَرُوا۟ يُكَذِّبُونَ
٢٢ وَٱللَّهُ أَعْلَمُ بِمَا يُوعُونَ ٢٣ فَبَشِّرْهُم بِعَذَابٍ أَلِيمٍ ٢٤
إِلَّا ٱلَّذِينَ ءَامَنُوا۟ وَعَمِلُوا۟ ٱلصَّٰلِحَٰتِ لَهُمْ أَجْرٌ غَيْرُ مَمْنُونٍ ٢٥

azikamwa amene ayandikitsidwa (kwa Allah ku jannah osati ena).

22-28 [Ndithu anthu ovomereza ndi kumvera Allah akakhala mu jannah akusangalala. Akakhala pa makama akuyang'ana kwa Mbuye wawo ndi ku zomwe awalinganizira mu zabwinozabwino. Ukaona pa nkhope zawo chimwemwe cha mtendere. Akamwetsedwa kuchokera mu mowa woyera ziwiya zake zotsekedwa bwino mapeto ake kuli fungo la misk. Ndipo mu mtendere wamuyayawo apikisanire opikisana. Chakumwa chimenechi chosakanizira chake chikakhala chochokera ku mtsinje wa ku jannah wotchedwa tasniim. Uwu ndi mtsinje umene udakonzedwa kuti azikamwa m'menemo awo amene ali oyandikitsidwa, ndikuti asangalale nawo.]

(29) Ndithu, amene adachita machimo adali kuwaseka (mwachipongwe) okhulupirira (pa dziko lapansi);

(30) (okhulupirira) akadutsa pafupi ndi iwo ankakodolerana maso (mwa chipongwe)

(31) Ndipo akabwerera kwa anzawo amabwerera akusangalala (ndi kunyozedwa kwa okhulupirira;

(32) Ndipo (nthawi zonse) akawaona (Asilamu) amanena: "Ndithu, awa ndi osokera (chifukwa chokhulupirira Muhammad (SAW)."

(33) Sadaperekedwe (akafiri) kukhala ayang'aniri (aakulu kwa okhulupiririra ndi kuwaweluza za kulungama ndi kusokera).

(34) Basi pa tsikuli okhulupirira adzaseka osakhulupirira (powabwezera chipongwe chawo chimene ankachita pa dziko lapansi).

29-34 [Ndithu anthu amene adachita zoipa adali pa dziko lapansi akuchitira chipongwe anthu okhulupirira. Akawadutsa iwowo amaphethirirana maso mowachita chipongwe iwowo. Ndipo akabwerera anthu oipitsawa kwa anthu awo ndi abale awo. Akumasangalala nawo mwachipongwe chowachita anthu okhulupirira. Ndipo makafiri amenewa akawaona maswahaba a Muhammad (SAW) ndipo adatsata chiongoko, akunena kuti: "Ndithu awa ndi osokera mukutsatira kwawo Muhammad (SAW)". Ndipo sadatumizidwe awa oipitsawa kukhala ayang'aniri a maswahaaba a Muhammad (SAW). Ndipo tsiku la Kiyama adzachita chipongwe anthu amene adamuvomereza Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndi kugwiritsa ntchito malamulo Ake (kuwabwezera) makafiri monga m'mene ankawachitira chipongwe makafiri pa dziko lapansi.]

(35) Atakhala pa mipando ya ulemeu uku akuyang'ana (mtendere umene Allah wawapatsa).

(36) Kodi alipidwa osakhulupirira pa zomwe ankachita zija (pa dziko lapansi)?

34-35 [Pa mabwalo a ulemerero azikayang'ana anthu okhulupirira ku zomwe Allah wawapatsa mu maulemerero ndi mtendere mu jannah. Ndipo zazikulu kuposa apo ndiko kuona nkhope yolemekezeka ya Allah. Kodi alipidwa makafiri – poti iwo achitiridwa zimenezo- malipiro woyenerera ndi zomwe adali kuzichita pa dziko lapansi mu zoipa ndi machimo?]

## (84) SUURAT-UL-INSHIQAAQ

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Pamene thambo lidzang'ambike (kusonyeza mapeto ake),

(2) Ndikudzamvera lamulo la Mbuye wake; ndipo lidzayenera kutero,

(3) Ndiponso pamene nthaka idzatambasulidwe (pogumuka mapiri ake ndi kuchoka zitunda zake).

(4) Ndi kutaya zomwe zidali m'kati mwake (monga maliro ndi miyala ya mtengo wapatali) ndikukhala yopanda kanthu.

(5) Ndi kudzamvera lamulo la Mbuye wake, ndipo lidzayenera kutero, (choncho zikadzachitika zimenezi ndiye kuti munthu adzalandira mphoto ya zochita zake).

1-5 [Pamane thambo lidzang'ambike ndi kuonongeka ndi mitambo Tsiku la Kiyama, ndi pamene lidzamvere lamulo la Mbuye wake zomwe adzalilamule mu zong'ambika, ndipo lidzayenerera kuti limvere lamulo Lake. Ndipo pamene nthaka idzatambasulidwe ndi kukuzidwa, mapiri ake naperekapereka mu tsiku limenelo, ndi kuponyedwa kunja zomwe zili m'kati mwake mu zinthu zakufa, ndi kusiyana nazo, komanso litamvera lamulo la Mbuye wake mu zomwe adzailamule, ndipo idzayenerera kumvera lamulo Lakelo.]

(6) E, iwe munthu! Ndithudi iwe ukubwerera kwa Mbuye wako ndi zochita zako (zabwino kapena zoipa). Kubwera kotsimikizika, ndipo iwe ukumana ndi zotsatira za zichitochito zako.

[E, iwe munthu! Ndithu iwe ukuyenda kupita kwa Allah ndipo ukugwira ntchito zabwino komanso zoipa, kenako ukakumana ndi Allah Tsiku la Kiyama nadzakulipira ntchito zako kudzera mu ubwino Wake kapena chilungamo Chake].

(7) Tsono amene adzapatsidwe kaundula wake (wa zochita zake) ku dzanja la manja,

(8) Basi iye, adzawerengeredwa, kuwerengeredwa kopepuka, kofewa.

(9) Ndipo adzabwerera kwa anthu ake (okhulupirira) ali wokondwa.

7-9 [Ndipo munthu amene adzapatsidwe kaundula wa ntchito zake ku dzanjadzanja kwake, iye ali womukhulupirira Mbuye wake, ndiye kuti adzawerengedwa kuwerengedwa kosavuta ndipo adzabwerera kwa abale ake ku jannah ali wosangalala.]

(10) Koma yemwe adzapatsidwe kaundula wake (wa zochita zake) cha kumanzere kudzera kumbuyo kwa msana wake (chifukwa chomunyoza),

(11) Basi iye adzaitana imfa (kuti imufikire kuti afe apumule, koma siidzamufikira).

(12) Ndipo adzalowa ku moto woyaka.

(13) Kamba kakuti iye adali wokondwa , (kukondwa kwa machimo) pamodzi ndi anthu ake (osaganizira za mathero ake).

(14) Ndithudi, amaganiza kuti zadzabwerera (kwa Allah ndiponso sadzawerengedwa.)

(15) Chifukwa ninji (asabwerere)? Mbuye wake adali kumuona (choncho alipidwa zimene adachita).

10-15 [Ndipo munthu amene adzapatsidwe kaundula wa ntchito zake kudzera kuseli kwa msana wake, ameneyo ndi amene ali wokanira Allah, ndiye adzaitana chionongeko ndi imfa , ndipo adzalowa ku moto ndi kukaotchedwa ndi kutentha kwake. Ndithu iye adali mu anthu ake pa dziko lapansi ali wosangalala, wonyengeka, wosaganizira za mapeto. Ndithu iye amaganiza kuti sadzabwerera kwa Mulengi wake ali wamoyo kuti akamuwerengere. Zingachitike bwanji zimenezo, ndithudi Allah adzamubwezera kwa Iye monga m'mene adamuyambira ndi kudzamulipira ntchito zake. Ndithu Mbuye wake za iye ali Woyang'anitsitsa, Wodziwa za iye kuchokera tsiku limene adamulenga kufikira atamuukitsanso kwa akufa.]

(16) Ndikulumbirira kufiira kwa dzuwa (pamene likulowa).

(17) Ndi usiku ndi zimene wasonkhanitsa (mu mdima mwake, monga anthu, nyama ndi zina zotero),

(18) Ndi mwezi ukakwanira dangalira (lake).

(19) Mudzachoka apa kunka apa (pa umoyo uno mpakana umene uli nkudza).

16-19 [Allah Taalaa walumbirira kufiira kwa chizimezime nthawi yolowa dzuwa. Ndi usiku ndi zimene wasonkhanitsa mu nyama ndi zoulukauluka ndi zokwawa ndi zina zotero. Ndi mwezi pamene ukukwanira dangalira lake, ndithudi mudzayenda -inu anthu- masitepemasitepe ochuluka ndi kakhalidwe kotayanatayana kuchokera ku dontho la umuna kufika ku ntchintchi ya magazi, kenako kufika ku mnofu , kukafikanso ku kuuziridwa mzimu kenako kupita ku imfa kenakonso kupita kwa kuuka kwa akufa ndi kuukitsidwa. Sizovomerezeka kwa cholengedwa kulumbirira china chake chosakhala Allah, iye atachita izi adzakhala kuti waphatikiza Allah ndi zina zake pa ibaadah.]

(20) Kodi n'chiyani chikuwaletsa awa (okanira) kukhulupirira (Allah ndi kuuka kwa akufa, zisonyezo zake zitaonekera poyera)?

(21) Ndipo ikawerengedwa kwa iwo Qur'aan, sakudzichepetsa (pogwetsa nkhope zawo pansi).

(22) Koma amene sadakhulupirire akutsutsa basi (chifukwa cha makani ndi kudzikweza).

(23) Ndipo Allah akudziwa (bwinobwino) zimene akuzisonkhanitsa.

(24) Choncho, auze nkhani ya chilango chopweteka.

(25) Kupatula awo amene akhulupirira ndi kuchita ntchito zabwino, kwa iwo kuli malipiro osatha.

20-25 [Ndi chinthu chanji chimene chikuwaletsa kukhulupirira mwa Allah ndi Tsiku Lomaliza pambuyo poti zizindikiro zaonekera kwa iwo? Ndi chifukwa chiyani ikawerengedwa Qur'aan kwa iwo sakugwetsa nkhope zawo pansi komanso osazikhulupirira zimene zadza m'menemo? Ndithudi chikhalidwe cha anthu okanira ndi kutsutsa ndi kusemphana nacho choonadi. Ndipo Allah ndi Wodziwa zimene akuzibisa m'zifuwa zawo za mankhalu chonsecho ndi kuzindikira kwawo koti ndithu zimene yadza nazo Qur'aan ndi zoona choncho iwe Mtumiki (SAW) apatse nkhani yonyazitsa

سُورَةُ البُرُوجِ — ترتيبها ٨٥ — آياتها ٢٢

بِسْمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحْمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

وَٱلسَّمَآءِ ذَاتِ ٱلْبُرُوجِ ﴿١﴾ وَٱلْيَوْمِ ٱلْمَوْعُودِ ﴿٢﴾ وَشَاهِدٍ وَمَشْهُودٍ
﴿٣﴾ قُتِلَ أَصْحَٰبُ ٱلْأُخْدُودِ ﴿٤﴾ ٱلنَّارِ ذَاتِ ٱلْوَقُودِ ﴿٥﴾ إِذْ هُمْ عَلَيْهَا
قُعُودٌ ﴿٦﴾ وَهُمْ عَلَىٰ مَا يَفْعَلُونَ بِٱلْمُؤْمِنِينَ شُهُودٌ ﴿٧﴾ وَمَا نَقَمُوا۟
مِنْهُمْ إِلَّآ أَن يُؤْمِنُوا۟ بِٱللَّهِ ٱلْعَزِيزِ ٱلْحَمِيدِ ﴿٨﴾ ٱلَّذِى لَهُۥ مُلْكُ
ٱلسَّمَٰوَٰتِ وَٱلْأَرْضِ ۚ وَٱللَّهُ عَلَىٰ كُلِّ شَىْءٍ شَهِيدٌ ﴿٩﴾ إِنَّ ٱلَّذِينَ
فَتَنُوا۟ ٱلْمُؤْمِنِينَ وَٱلْمُؤْمِنَٰتِ ثُمَّ لَمْ يَتُوبُوا۟ فَلَهُمْ عَذَابُ جَهَنَّمَ وَلَهُمْ
عَذَابُ ٱلْحَرِيقِ ﴿١٠﴾ إِنَّ ٱلَّذِينَ ءَامَنُوا۟ وَعَمِلُوا۟ ٱلصَّٰلِحَٰتِ لَهُمْ
جَنَّٰتٌ تَجْرِى مِن تَحْتِهَا ٱلْأَنْهَٰرُ ۚ ذَٰلِكَ ٱلْفَوْزُ ٱلْكَبِيرُ ﴿١١﴾ إِنَّ بَطْشَ
رَبِّكَ لَشَدِيدٌ ﴿١٢﴾ إِنَّهُۥ هُوَ يُبْدِئُ وَيُعِيدُ ﴿١٣﴾ وَهُوَ ٱلْغَفُورُ ٱلْوَدُودُ ﴿١٤﴾
ذُو ٱلْعَرْشِ ٱلْمَجِيدُ ﴿١٥﴾ فَعَّالٌ لِّمَا يُرِيدُ ﴿١٦﴾ هَلْ أَتَىٰكَ حَدِيثُ ٱلْجُنُودِ
﴿١٧﴾ فِرْعَوْنَ وَثَمُودَ ﴿١٨﴾ بَلِ ٱلَّذِينَ كَفَرُوا۟ فِى تَكْذِيبٍ ﴿١٩﴾ وَٱللَّهُ مِن
وَرَآئِهِم مُّحِيطٌۢ ﴿٢٠﴾ بَلْ هُوَ قُرْءَانٌ مَّجِيدٌ ﴿٢١﴾ فِى لَوْحٍ مَّحْفُوظٍ ﴿٢٢﴾

سُورَةُ الطَّارِقِ — ترتيبها ٨٦ — آياتها ١٧

yoti ndithu Allah wapamwambamwamba wawakonzera iwowo chilango chowawitsa koma anthu amene adakhulupirira mwa Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndikuchita zomwe Allah walamulira kuzichita, ali nawo malipiro Tsiku Lomalia osadukiza komanso osapunguka.]

## (85) SUURAT-UL- BURUUJ

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Ndikulumbirira thambo lomwe liri ndi buruuj (nyenyezi zikuluzikulu).

(2) Ndi tsiku lolonjezedwa (kuwerengedwa ndi kulipidwa).

(3) Ndi woikira umboni, ndi woikiridwa umboni.

(4) Atembereredwa eni ngalande za moto (zomwe adali kuwazunzira okhulupirira Allah, achimuna ndi achikazi).

(5) (Ngalande) za moto wankhuni (zambiri zomwe adali kuzikoleza ndi kuotchera okhulupirira).

(6) Pamene iwo adali chikhalire m'mphepete mwa ngalande za moto.

(7) Uku iwo akuyang'ana zomwe amawachitira okhulupirira (pootchedwa ndi moto).

(8) Sadaone (chilichonse) choipa mwa iwo koma chifukwa choti adakhulupirira Allah Mwini mphamvu zonse ndiponso Mwini kuyamikidwa.

(9) Yemwe ufumu wa kumwamba ndi pansi ndi Wake; ndipo Allah ndi Mboni pa chilichonse.

1-9 [Allah walumbirira thambo lomwe lili ndi malo otsikirapo amene dzuwa ndi mwezi amawadutsa, komanso walumbirira Tsiku Lakiyama lomwe Allah walonjeza zolengedwa kuti adzazisonkhanitsa m'tsikulo. Komanso walumbirira woikira umboni akamaikira ndinso woikiridwa umboni akamaikiridwa. Ndipo Allah Subhaanahu amalumbirira zimene wazifuna mu zolengedwa Zake, tsono cholengedwa ndiye nkosaloledwa kwa icho kulumbirira wina wake wosakhala Allah popeza ndithu kulumbirira china chake chosakhala Allah ndi shirk. Atembereredwa anthu amene adakumba pansi ngalande yaikulu yolangiramo anthu okhulupirira komanso adayatsamo moto waukali woyaka zedi. Pa nthawi imene iwo adali chikhalire pa ngalandezo osasiyana nazo ndipo iwo pa zomwe akuwachita anthu okhulupirira mu zopereka mazunzo ndi kwalanga anali pompo. Ndipo palibe chifukwa china chimene adawalangira iwowo ndi chilango chopweteka chamtundu uwu kupatula kuti iwowo adali okhulupirira mwa Allah Wamphamvu Amene sagonjetsedwa, Woyamikidwa mu zoyankhula, zochita ndi mbiri Zake Amene ndi Wake ufumu wa kumwamba ndi pansi. Ndipo Iye Subhaanahu pa chinthu chilichonse akuchiona palibe chimene chingabisike kwa Iye.]

(10) Ndithu, amene ayesa mayeso okhulupirira achimuna ndi achikazi (pa chipembedzo chawo ndi mazunzo ndi chilango cha moto), pambuyo pake osalapa (pa zimenezi) adzalandira chilango cha jahena ndiponso chilango cha moto wopsereza (chifukwa chootcha okhulupirira).

[Ndithu anthu amene adawaotcha anthu okhulupirira achimuna ndi achikazi ndi moto chifukwa choti awapotoloze asiye chipembedzo cha Allah, kenako napanda kulapa, ali nacho Tsiku Lomaliza chilango cha jahena komanso ali nacho chilango champhamvu chowaotcha.]

(11) Ndithudi amene akhulupirira ndi kuchita ntchito zabwino, adzakhala ndi minda (momwe) mitsinje ikuyenda pansi pake (mtendere) umenewo ndiko kupambana kwakukulu.

[Ndithu anthu amene adamuvomereza Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndi kugwira ntchito zolungama, ali nayo minda yomwe ikuyenda pansi pa nyumba zake za chifumu mitsinje, kumeneko ndiko kupambana kwakukulu.]

(12) Ndithu, kulanga kwa Mbuye wako (kwa anthu achinyengo) , ndi kwaukali kwambiri.

(13) Iye (m'modzi Yekha) ndi Amene adayambitsa zolengedwa ndiponso ndi Yemwe adzazibweza (pambuyo poonongeka);

(14) Iye, ndi Wokhululuka (kwa amene walapa kwa Iye), ndiponso wokonda kwambiri (amene akum'konda ndi kumumvera).
(15) Mwini mpando wachifumu (ndiponso) Wolemekezeka (m'mene alili ndi mbiri Zake).
(16) Wochita zimene wafuna (ndipo chimene wafuna sichikanika).
12-16 [Ndithu kubwezera kwa chilango cha Mbuye wako kwa adani Ake ndi kuwalanga Kwake kwa iwowo ndi kwakukulu zedi. Iye ndi Amene adayambitsa zolengedwa kenako nazibwezeretsa. Ndipo Iye ndi Wokhululuka kwa amene walapa. Wochulukitsa chikondi kwa abwenzi Ake. Mwini mpando waulemerero ndiponso Wopatsa amene wafika mapeto mu ubwino ndi kuwolowa manja. Wochita zimene wafuna palibe chinthu chimene wafuna chimene chingakane kwa Iye.]
(17) Kodi yakufika nkhani ya magulu a nkhondo,
(18) Firiaun (Farao) ndi Samudu (ndi chilango chimene chidawapeza chifukwa chakulimbira kwawo pa zinthu zopanda pake)?
(19) Koma amene sadakhulupirire ali mkati motsutsa basi.
(20) Koma Allah awazinga mbali zonse.
(21) Koma iyi ndi Qur'aan yolemekezeka (imene ikusonyeza kulungama kwako).
(22) Yomwe idachokera mu ubawo wotetezedwa (chisileti chachikulu) wotetezedwa [ndi manja aliwonse, wosintha kanthu kapena kuonjezerapo.]
17-22 [Kodi iwe Mtumiki (SAW) yakufika nkhani ya magulu okanira Allah otsutsa Atumiki Ake, Firiaun ndi Samuda ndi zomwe zidawapeza za chilango ndi mazunzo koma anthu sadaganizire zimenezo. Koma kuti anthu amene adakana ali mu kutsutsa kopitirira monga mwa khalidwe la anthu amene adadza iwo asadabwere. Ndipo Allah wawazinga iwowo powadziwa komanso kuthekera Kwake palibe chobisika chilichonse kwa Iye mwa iwo komanso ntchito zawo. Ndipo Qur'aan siili monga akunenera anthu abodzawa opembedza mafanowa kuti ndi ndakatulo ndi ufiti kotero iwo ayikanira, koma imeneyi ndi Qur'aan yaikulu yolemekezeka. Ili mu Kaundula Wamkulu wosungika palibe kumupeza kusemphanitsa kulikonse kapena kusintha.]

## (86) SUURAT – ALTWAARIQ

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**
(1) Ndikulumbirira kumwamba ndi nyenyezi zimene zimadza usiku,
(2) Chitakudziwitse n'chiyani nyenyezi zodza usikuzo?
(3) Imeneyo ndi nyenyezi yowala kwambiri (mu mdima).

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

وَٱلسَّمَآءِ وَٱلطَّارِقِ ١ وَمَآ أَدۡرَىٰكَ مَا ٱلطَّارِقُ ٢ ٱلنَّجۡمُ ٱلثَّاقِبُ ٣ إِن كُلُّ
نَفۡسٖ لَّمَّا عَلَيۡهَا حَافِظٞ ٤ فَلۡيَنظُرِ ٱلۡإِنسَٰنُ مِمَّ خُلِقَ ٥ خُلِقَ مِن مَّآءٖ
دَافِقٖ ٦ يَخۡرُجُ مِنۢ بَيۡنِ ٱلصُّلۡبِ وَٱلتَّرَآئِبِ ٧ إِنَّهُۥ عَلَىٰ رَجۡعِهِۦ لَقَادِرٞ ٨
يَوۡمَ تُبۡلَى ٱلسَّرَآئِرُ ٩ فَمَا لَهُۥ مِن قُوَّةٖ وَلَا نَاصِرٖ ١٠ وَٱلسَّمَآءِ ذَاتِ ٱلرَّجۡعِ ١١
وَٱلۡأَرۡضِ ذَاتِ ٱلصَّدۡعِ ١٢ إِنَّهُۥ لَقَوۡلٞ فَصۡلٞ ١٣ وَمَا هُوَ بِٱلۡهَزۡلِ ١٤ إِنَّهُمۡ
يَكِيدُونَ كَيۡدٗا ١٥ وَأَكِيدُ كَيۡدٗا ١٦ فَمَهِّلِ ٱلۡكَٰفِرِينَ أَمۡهِلۡهُمۡ رُوَيۡدَۢا ١٧

### سُورَةُ الأَعۡلَى
ترتيبها ٨٧ — آياتها ١٩

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

سَبِّحِ ٱسۡمَ رَبِّكَ ٱلۡأَعۡلَى ١ ٱلَّذِي خَلَقَ فَسَوَّىٰ ٢ وَٱلَّذِي قَدَّرَ فَهَدَىٰ
٣ وَٱلَّذِيٓ أَخۡرَجَ ٱلۡمَرۡعَىٰ ٤ فَجَعَلَهُۥ غُثَآءً أَحۡوَىٰ ٥ سَنُقۡرِئُكَ
فَلَا تَنسَىٰٓ ٦ إِلَّا مَا شَآءَ ٱللَّهُۚ إِنَّهُۥ يَعۡلَمُ ٱلۡجَهۡرَ وَمَا يَخۡفَىٰ ٧ وَنُيَسِّرُكَ
لِلۡيُسۡرَىٰ ٨ فَذَكِّرۡ إِن نَّفَعَتِ ٱلذِّكۡرَىٰ ٩ سَيَذَّكَّرُ مَن يَخۡشَىٰ ١٠
وَيَتَجَنَّبُهَا ٱلۡأَشۡقَى ١١ ٱلَّذِي يَصۡلَى ٱلنَّارَ ٱلۡكُبۡرَىٰ ١٢ ثُمَّ لَا يَمُوتُ
فِيهَا وَلَا يَحۡيَىٰ ١٣ قَدۡ أَفۡلَحَ مَن تَزَكَّىٰ ١٤ وَذَكَرَ ٱسۡمَ رَبِّهِۦ فَصَلَّىٰ ١٥

1 (4) Ndithudi palibe mzimu uliwonse koma uli ndi msungi wake (amene akuuyang'anira ndi kulemba zonse zochita zake).
1-4 [Allah Subhaanahu walumbirira thambo komanso nyenyezi imene imabwera usiku. Ndipo kodi ndi chiyani chitakudziwitse ukulu wa nyenyezi imeneyi? Imeneyo ndi nyenyezi yowala kwambiri. Palibe mzimu uliwonse pokhapokha kuti udaikidwira mngero wouyang'anira, wousungira ntchito zake kuti adzawerengeredwe nazo Tsiku la Kiyama.
(5) Aganizire munthu, kodi adalengedwa ndi chiyani?
(6) Adalengedwa kuchokera ku madzi otwamphuka.
(7) Amatuluka (kuchokera pakati pa mafupa a msana ndi chifuwa {nthiti} a munthu wamwamuna ndi wamkazi).
(8) Ndithu Iye ndi Wakutha kubwezanso (ku moyo pambuyo pa imfa).
5-8 [Ndipo munthu wokanira za kuuka kwa akufa ayang'ane kuti kuchokera ku zinthu zanji adalengedwa kuti adziwe kuti ndithu kubwezeretsa kulenga kwa munthu sikovuta

kuposa kumulenga kwake pa nthawi yoyambirira. Adalengedwa kuchokera ku umuna umene umadonthetsedwa mwa mphamvu mu chiberekero umene umatuluka kuchokera ku msana wa mwamuna ndi chifuwa cha wamkazi. Ndithu Amene adalenga munthu kuchokera ku madzi ali nako kuthekera komubwezeretsanso ku moyo pambuyo pa imfa.]
9 Tsiku limene zobisika zonse zidzaonekere poyera.
10 Munthu sadzakhala ndi mphamvu (tsiku limenelo zodzitetezera iye mwini) ndiponso sadzakhala ndi mtetezi.
9-10 [Tsiku limene zobisika zidzayesedwe ndi kuwululidwa m'mene adazibisira ndipo sidzalekanitsidwa mu zimenezo zolungama ku zomwe zili zoipa. Ndipo munthu sadzakhala ndi mphamvu yodzitetezera iye mwini ku zimenezo ndiponso sadzakhala ndi mthandizi womutsekereza ku chilango cha Allah.]
11 Ndikulumbiriranso mitambo ya mvula yobweretsabweretsa mvula.
12 Ndi nthaka imene imang'ambika (potulutsa m'mera).
13 Ndithudi iyi (Qur'aan) ndi mawu olekanitsa (pakati pa choonadi ndi chabodza)
14 Imeneyi sinkhambakamwa.
11-14 [Ndikulumbirira thambo la mvula yobweretsabweretsa. Ndiponso ndikulumbirira nthaka imene imang'ambika ndi zomwe imachita kuti zitulukemo zomeramera. Ndithu Qur'aan ndi liwu la chigamulo pakati pa choonadi ndi chabodza. Ndipo imeneyi sinkhambakamwa ayi. Ndipo nkosaloledwa kwa cholengedwa kulumbirira china chake chosakhala Allah ndipo atati atero ndiye kuti wachita shirk.]
15 Ndithudi iwo akukonza chiwembu.
16 Nanenso ndikuwakonzera chiwembu (champhamvu kwambiri chimene sangathe kuchipewa).
17 Basi, apatse nthawi osakhulupirira, apatse nthawi pang'ono (aona posachedwa).
15-17 [Ndithu anthu omutsusa Mtumiki (SAW) ndi Qur'aan akumakonza ndi kulinganiza chiwembu kuti ndi chiwembu chawocho atsekereze choonadi ndi kuthandizira chonama. Inenso ndikukonza chiwembu chotulutsira poyera choonadi ngakhale makafiri atadana nazo. Ndiye iwe Mtumiki (SAW) usawafulumizitsire popempha kuti chiwatsikire chilango iwowo ayi, koma apatseko kampata ndipo uwayembekezere pang'ono ndipo usawapupulumire ndipo udzaona zimene zidzawapeze iwowo mu chilango, mazunzo ndi chionongeko].

## (87) SUURAT-UL- AALAA

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**
1 Lemekeza dzina la Mbuye wako wa Pamwambamwamba (ndi kuliyeretsa ku zinthu zosayenera).
2 Amene adalenga (chilichonse) ndi kuchikonza bwinobwino (m'kalengedwe kolingana).
3 Amene adalamuliratu (chilichonse zochita zake) ndi kuchiongolera zomuyenereza pa chilengedwe chake).
4 Ndi Yemwenso akumeretsa msipu (m'nthaka, umene nyama zimadya);
5 Ndipo nausandutsa kukhala wouma ndi wodera.
1-5 [Liyeretse dzina la Mbuye wako wa Pamwambamwamba ku wothandizana naye komanso ku kupunguka kuyeretsa koyenerera ndi ukulu Wake Subhaanahu, Amene adalenga zolengedwa zonse ndipo adazilenga mwaluso kalengedwe kake ndipo adachita dongosolo labwino. Ndipo Iye ndi Amene adakonzeratu zonse zolinganizidwa kotero adawongolera cholengedwa chilichonse ku zomwe zingachiyenerere. Ndiponso Iye ndi Amene amameretsa msipu wobiriwira ndipo pambuyo pake amauchita kukhala wouma, woderako, wosanduka.]
6 Tikulakatulira (chivumbulutso Chathu) ndipo siuiwala.
7 Kupatula chimene wafuna Allah (kuti uchiiwale); ndithu Iye amadziwa zoonekera ndi (zimene) zimabisika.
6-7 [Tikuwerengera iwe Mtumiki (SAW) Qur'aan imeneyi kukuwerengera koti siungakuiwale kupatuka zimene wafuna Allah mu zimene zagamulidwa ndi nzeru Zake zakuya kuti amuiwalitse chifukwa chofuna kukonza chabwino chimene akuchidziwa Iye. Ndithu Iye Subhaanahu akudziwa zoonekera mu zoyankhula ndi zochitika ndipo ziwirizi sizingabisike kwa Iye.]
8 Ndipo tikufewetsera (njira yochitira zinthu) zabwino. [Ndipo tikufewetsera zinthu zofewa mu zinthu zako zonse zina mwa izo kukufewetsera kunyamula mtolo wolemetsa wa utumiki ndipo adachichita chipembedzo chako kukhala chofewa mopandamo chovuta.]
9 Akumbutse (anthu powalalikira) ngati kukumbutsa kuthandiza. [Choncho uwalalikire anthu ako iwe Mtumiki (SAW) mofanana ndi momwe takufewetsera iwe ndi zomwe zikuvumbulutsidwa kwa iwe. Ndipo usankhe ndi chikumbutsochi anthu amene ukuyembekezera kwa iye kuganizira. Ndipo usadzivutitse mu mtima mwako pokumbutsa munthu amene chikumbutso sichingamupatse kena kalikonse kupatula mankhalu ndi kutalikira.]

(10) (Palibe chikaiko ulalikiwo) aukumbukira (ndi kuthandizidwa nawo) amene akuopa Allah).
(11) Ndipo wa mavuto ambiri (wamakani) adzitalikitsa ndi ulalikiwo.
(12) Amene adzalowa ku moto waukulu (umene wakonzedwa kuti udzakhale malipiro ake).
(13) Ndipo sakafa m'menemo (ndi kupulumuka ku mazunzo) ndiponso sakakhala ndi moyo (wamtendere).
10-13 [Apeza ulaliki munthu amene akuopa Mbuye wake, ndipo adzatalikitsidwa ku ulalikiwu munthu wamankhalu amene saopa Mbuye wake, amene adzalowe ku moto waukulu wa jahena ndipo akavutitsidwa ndi kuotcha kwake, kenako sakafa m'menemo moti n'kupuma komanso sakakhala ndi moyo woti ndikumuthandiza.]
(14) Ndithu, wapambana amene wadziyeretsa (ku machimo).
(15) Ndi kukumbukira dzina la Mbuye wake (ndi mtima wake komanso lirime lake) uku akumapemphera.
14-15 [Ndithudi wapambana munthu amene wauyeretsa mzimu wake ku makhalidwe oipa, ndipo nakumbuka Allah, ndipo naulemekeza uyekha Wake ndi kumamupempha komanso kugwira ntchito zomwe zingamusangalatse Iye, komanso namapemphera swalaat zonse mu nthawi yake pofuna chiyanjo cha Allah komanso kutsatira malamulo Ake.]
(16) Koma inu mukonda kwambiri moyo wa dziko lapansi. [Ndithudi inu anthu mumakonda zokongoletsa za dziko lapansi koposa mtendere wa Tsiku Lomaliza].
(17) Pamene (moyo wa) Tsiku Lomaliza ndi wabwino kwambiri ndiponso wamuyaya. [Ndipo nyumba ya Tsiku Lomaliza ndi zomwe zili m'menemo mu mautendere osatha ndi zabwino kuposa dziko lapansi komanso ndi zamuyaya.]
(18) Ndithu izi (mukuwuzidwazi mu Qur'aan) zilipo m'mabuku oyamba, akale.
(19) Mabuku a Ibrahim (AS) ndi Mussa (AS).
18-19 [Ndithu zimene mwauzidwazi mu suurah imeneyi ndi zimene zatsimikizika tanthauzo lake mu mabuku amene adavumbulutsidwa Qur'aan isadadze amenewo ndi mabuku a Ibrahim (AS) ndi Mussa (AS).

## (88) SUURAT-UL-GHAASHIYAT

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Kodi yakudzera (iwe Muhammad SAW) nkhani (ya Kiyama) imene idzaphimba (anthu ndi zoopsa zake)? [Kodi yakufika iwe Mtumiki (SAW) nkhani ya Kiyama imene idzaphimbe anthu ndi zoopsa zake?]

بَلْ تُؤْثِرُونَ الْحَيَاةَ الدُّنْيَا ﴿١٦﴾ وَالْآخِرَةُ خَيْرٌ وَأَبْقَىٰ ﴿١٧﴾ إِنَّ
هَٰذَا لَفِي الصُّحُفِ الْأُولَىٰ ﴿١٨﴾ صُحُفِ إِبْرَاهِيمَ وَمُوسَىٰ ﴿١٩﴾

ترتيبها ٨٨ — سُورَةُ الغَاشِيَةِ — آياتها ٢٦

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَٰنِ الرَّحِيمِ

هَلْ أَتَاكَ حَدِيثُ الْغَاشِيَةِ ﴿١﴾ وُجُوهٌ يَوْمَئِذٍ خَاشِعَةٌ ﴿٢﴾
عَامِلَةٌ نَّاصِبَةٌ ﴿٣﴾ تَصْلَىٰ نَارًا حَامِيَةً ﴿٤﴾ تُسْقَىٰ مِنْ عَيْنٍ آنِيَةٍ ﴿٥﴾
لَّيْسَ لَهُمْ طَعَامٌ إِلَّا مِن ضَرِيعٍ ﴿٦﴾ لَّا يُسْمِنُ وَلَا يُغْنِي مِن جُوعٍ ﴿٧﴾
وُجُوهٌ يَوْمَئِذٍ نَّاعِمَةٌ ﴿٨﴾ لِّسَعْيِهَا رَاضِيَةٌ ﴿٩﴾ فِي جَنَّةٍ عَالِيَةٍ ﴿١٠﴾
لَّا تَسْمَعُ فِيهَا لَاغِيَةً ﴿١١﴾ فِيهَا عَيْنٌ جَارِيَةٌ ﴿١٢﴾ فِيهَا سُرُرٌ مَّرْفُوعَةٌ ﴿١٣﴾
وَأَكْوَابٌ مَّوْضُوعَةٌ ﴿١٤﴾ وَنَمَارِقُ مَصْفُوفَةٌ ﴿١٥﴾ وَزَرَابِيُّ مَبْثُوثَةٌ ﴿١٦﴾
أَفَلَا يَنظُرُونَ إِلَى الْإِبِلِ كَيْفَ خُلِقَتْ ﴿١٧﴾ وَإِلَى السَّمَاءِ كَيْفَ
رُفِعَتْ ﴿١٨﴾ وَإِلَى الْجِبَالِ كَيْفَ نُصِبَتْ ﴿١٩﴾ وَإِلَى الْأَرْضِ كَيْفَ
سُطِحَتْ ﴿٢٠﴾ فَذَكِّرْ إِنَّمَا أَنتَ مُذَكِّرٌ ﴿٢١﴾ لَّسْتَ عَلَيْهِم
بِمُصَيْطِرٍ ﴿٢٢﴾ إِلَّا مَن تَوَلَّىٰ وَكَفَرَ ﴿٢٣﴾ فَيُعَذِّبُهُ اللَّهُ الْعَذَابَ
الْأَكْبَرَ ﴿٢٤﴾ إِنَّ إِلَيْنَا إِيَابَهُمْ ﴿٢٥﴾ ثُمَّ إِنَّ عَلَيْنَا حِسَابَهُم ﴿٢٦﴾

(2) Nkhope zina tsiku limenelo zidzakhala zonyozeka.
(3) Zogwira ntchito yotopetsa kwambiri (ku moto).
(4) Zikalowa ku moto wotentha kwambiri.
(5) Zikamwetsedwa a kasupe wotentha kwabasi
(6) Sadzakahala ndi chakudya koma m'mera wa minga (woipa umene akalangidwa nawo).
(7) Wosanenepetsa (thupi) ndiponso wosathetsa njala.
2-7 [Nkhope za makafiri tsiku limenelo zikakhala zonyozeka ndi chilango, zotopa ndi ntchito zolemetsa, moto woyaka kwambiri ukaotcha nkhope zimenezo, zikamwetsedwa kuchokera ku mtsinje wotentha kwambiri. Anthu a ku moto sakakhala ndi chakudya kupatula m'mera wa minga wokakamira pa nthaka chimenecho ndicho chakudya choipitsitsa komanso chonyansa chomwe sichinganenepetse thupi la wochidyayo kuti asanyentchere ayi komanso sichothetsa njala yake kapena ludzu lake].
(8) Nkhope zina tsiku limenelo zidzakhala zosangalala.
(9) Zidzakondweretsedwa ndi malipiro a zochita zawo (za dziko lapansi).

(10) M'minda ya pamwamba (jannah).
(11) Sizikamva m'menemo mawu oipa (otukwana ndi kulaula).
(12) M'menemo muli akasupe oyenda (okongola).
(13) M'menemo muli mabedi apamwamba.
(14) Ndi matambula oikidwa bwino (pa maso pawo).
(15) Ndi misamilo yoikidwa m'mizeremizere.
(16) Ndi mphasa (za mtengo wapatali –carpet) zoyalidwa ponseponse.
8-16 [Nkhope za anthu okhulupirira Tsiku la Kiyama zikakhala za mtendere, chifukwa cha ntchito zake pa dziko lapansi zomvera Allah ndiye zikakhala zokondweretsedwa mu Tsiku Lomaliza. Zikakhala mu jannah yapamwambamwamba malo ake komanso ulemerero wake. Sizikamva m'menemo liwu limodzi lopanda pake. M'menemo muli mitsinje imene madzi ake akuyenderera. M'menemo muli makama apamwamba komanso matambula okonzedwera kwa anthu omweramo zakumwa. Komanso muli misamilo yoikidwa m'mizeremizere ina pambali pa im'nzake, komanso muli zinsalu zoyala za mtengo wapatali zoyalidwa ponseponse (ma kalapeti a ulemu).
(17) (Kodi akunyozera kulingalira zisonyezo za Allah) sakuyang'ana ngamira idalengedwa motani?
(18) Ndi thambo (limene akuliona nthawi zonse) m'mene lidatukulidwira (kutali popanda mzati)?
(19) Ndi mapiri momwe adakhazikitsidwira (molimba)?
(20) Ndi nthaka momwe idayalidwira?
17- 20 [Kodi sakuona makafiri okanirawa ngamira kuti kodi idalengedwa motani cholengedwa chodabwitsachi? Ndiponso sakuona thambo m'mene lidatukuliridwira kutukula kochititsa kaso? Ndiponso mapiri m'mene adazikiridwira kotero kudapezeka chifukwa cha mapiriwo kulimba kwa nthaka ndi kukhazikika? Ndiponso nthaka m'mene idayaliridwira?]
(21) Choncho kumbutsa, ndithudi iwe ndiwe mkumbutsi.
(22) Siuli pa iwo mkakamizi.
21-22 [Choncho iwe Mtumiki (SAW) alalikire anthu osalabadirawa ndi zomwe udatumizidwa nazo kwa iwo, ndipo usadandaule kusalabadira kwawoko, ndithudi iwe ndi mlaliki wawo, sizili zoyenera kwa iwe kuwakakamizira pa chikhulupiriro.]
(23) Kupatula amene wanyoza n'kukanira.
(24) Ndiye Allah adzamulanga ndi chilango chachikulu.
23-24 [Koma amene wachipatsa msana wake chikumbutso ndi ulaliki napitirira pa ukafiri wakewo, ndiye kuti Allah adzamulanga ndi chilango chopweteka ku moto.]
(25) Ndithudi kwa Ife ndiko kobwerera kwawo.
(26) Kenako ndithudi kwa Ife ndi kumene kuli chiwerengero chawo.
25-26 [Ndithudi kwa Ife ndiko kobwerera kwawo pambuyo pa imfa,kenako ndithu kwa Ife ndi kumene kuli malipiro awo.]

## (89) SUURAT-UL-FAJR

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**
(1) Ndikulumbirira kuyera kwa m'bandakucha (pamene usiku ukuthawa).
(2) Ndi masiku khumi (a mwezi wa Dhul-Hijja omwe ndi opatulika kwa Allah).
(3) Ndi shaf'i ndi witri (nambala yogawika ndi yosagawika)
(4) Ndi usiku pamene ukupita (chifukwa cha kuyenda kwa dziko kodabwitsa).
(5) Kodi m'zimene zatchulidwazi simuli kulumbira kokwanira kwa munthu wanzeru?
1-5 [Allah Subhaanahu akulumbirira nthawi ya m'bandakucha komanso mausiku khumi oyambirira a mwezi wa Dhul-Hijja ndi zomwe zadza nazo, komanso walumbirira ziwiriziwiri zilizonse komanso chimodzichimodzi, komanso waulumbirira usiku ukamayenda ndi mdima wake, kodi polumbirira zinthu zimene zatchulidwazi simuli kukhutitsidwa kwa munthu wa nzeru?]
(6) Kodi sudadziwe momwe Mbuye wako adawalangira A'di (anthu a M'neneri Hudu AS)?
(7) A ku Irama: ataliatali ngati zipilala.
(8) Omwe onga iwo sadalengedwe m'maiko ena?
6-8 [Kodi siudadziwe iwe Mtumiki (SAW) momwe adachitira Mbuye wako ndi anthu a A'adi umene udali mtundu wa Irama, womwe udali wamphamvu ndi zomangamanga zonyamulidwa pa zipilala omwe sadalengedweko ofanana ndi iwo mu dziko mu kakulidwe ka matupi ndi mphamvu za nkhondo.?]
(9) (Kodi siudadziwe m'mene Allah adawalangira) Asamudu (anthu a m'neneri Swaleh AS) amene adali kudula matanthwe ku chigwa (chotchedwa Waadul-Qura ndi kumamanga nyumba zikuluzikulu)? [Ndi momwe adachitira ndi Asamudu anthu a Mtumiki Swaleh (AS) amene ankadula thanthwe mu chigwa ndi kuchita m'menemo nyumba?]
(10) Ndiponso (siudadziwe zomwe adam'chitira) Fir'aun (Farawo) mwini magulu a nkhodo (omwe amalimbikitsa ufumu wake monga m'mene zichiri zimalimbikitsira tenti). [Ndi momwe adam'chitira Fir'aun mfumu ya Eguputo mwini asilikali amene adalimbikitsa ufumu wake ndi kupereka mphamvu ku ulamuliro wake].
(11) Amene adaipitsa m'dziko mopyola malire?
(12) Ndipo adachulukitsa m'menemo kuononga (pamwamba pa kuononga).
(13) Choncho Mbuye wako adawathira ndi

mitundu ya zilango (zoopsa).

(14) Ndithu, Mbuye wako akulonda (zochita za anthu ndipo akuwasungira kuti adzawalipire).

11-14 [Anthu amenewa amene adali omva zaokha ndi kupondereza pa dziko la Allah nachulukitsa m'menemo chifukwa cha kupondereza kwawo kuononga. Ndipo Mbuye wako adathira pa iwo chilango chowawa. Ndithu Mbuye wako iwe Mtumiki (SAW) ali naye tcheru munthu amene akumunyoza, amamulekerera pang'ono kenako ndi kumulanga chilango champhamvu, chakuthekera.]

(15) Pamene munthu Mbuye wake akamuyesa (mayeso) ndi kumulemekeza ndi kum'patsa mtendere (wachuma, ulemerero ndi mphamvu) amanena monyada "Mbuye wanga wandilemekeza (chifukwa zimenezi n'zondiyenera ine).

[Tsono munthu ngati Mbuye wake atamuyesa mayeso ndi mtendere, ndi kumutambasulira iyeyo rizq lake, ndi kumuchita kukhala mu umoyo wabwino moposa, ndiye amaganiza kuti ndithu zimenezo zachitika chifukwa cha ulemerero wake kwa Mbuye wake, tero iye nkumati: "Mbuye wanga wandilemekeza"].

(16) Koma akamuyesa mayeso ndi kum'chepetsera riziq lake, amanena (motaya mtima): "Mbuye wanga wandinyoza". [Tsono akamuyesa mayeso nam'chepetsera iyeyo rizq lake, ndiye amaganiza kuti ndithu zimenezo zachitika chifukwa cha kupepuka kwake kwa Allah ndiye amanena: "Mbuye wanga wandinyoza"

(17) Sichoncho ayi (monga momwe mukuganizirira) koma inu simuchitira za ufulu ana amasiye.

(18) Ndipo simulimbikitsana za kudyetsa osauka,

(19) Ndipo mukudya chuma chamasiye, kudya kosusuka,

(20) Ndiponso mukukonda chuma kukonda kopyola muyeso.

17-20 [Zinthu sizili monga m'mene akuganizira munthu ameneyu koma kuti kulemekeza kumabwera chifukwa chomvera Allah komanso kuyalutsa kumadza chifukwa chomunyoza Iye. Ndipo inuyo simukulemekeza ana amasiye ndipo simukuwachitira zabwino pa kukhalirana nawo. Ndipo ena mwa inu salimbikitsa wina ndi mnzake zodyetsa anthu osauka. Ndipo mumadya magawo a ena pa ulowam'malo kudya kwambiri. Ndipo mumakonda chuma kukonda kolapitsa.]

(21) Sichoncho (siyani machitidwe amenewa) nthaka ikadzapondedwapondedwa (ndi kuifafaniza).

(22) Adzabwera Mbuye wako (m'mabweredwe omwe akuwadziwa Iye Mwini) ndipo angelo ali m'mizere.

(23) Ndipo tsiku limenelo idzabweretsedwa jahena

سُورَةُ الفَجۡرِ

ترتيبها ٨٩ — آياتها ٣٠

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

وَٱلۡفَجۡرِ ١ وَلَيَالٍ عَشۡرٖ ٢ وَٱلشَّفۡعِ وَٱلۡوَتۡرِ ٣ وَٱلَّيۡلِ إِذَا يَسۡرِ
٤ هَلۡ فِي ذَٰلِكَ قَسَمٞ لِّذِي حِجۡرٍ ٥ أَلَمۡ تَرَ كَيۡفَ فَعَلَ رَبُّكَ بِعَادٍ
٦ إِرَمَ ذَاتِ ٱلۡعِمَادِ ٧ ٱلَّتِي لَمۡ يُخۡلَقۡ مِثۡلُهَا فِي ٱلۡبِلَٰدِ ٨
وَثَمُودَ ٱلَّذِينَ جَابُواْ ٱلصَّخۡرَ بِٱلۡوَادِ ٩ وَفِرۡعَوۡنَ ذِي ٱلۡأَوۡتَادِ ١٠
ٱلَّذِينَ طَغَوۡاْ فِي ٱلۡبِلَٰدِ ١١ فَأَكۡثَرُواْ فِيهَا ٱلۡفَسَادَ ١٢ فَصَبَّ
عَلَيۡهِمۡ رَبُّكَ سَوۡطَ عَذَابٍ ١٣ إِنَّ رَبَّكَ لَبِٱلۡمِرۡصَادِ ١٤ فَأَمَّا
ٱلۡإِنسَٰنُ إِذَا مَا ٱبۡتَلَىٰهُ رَبُّهُۥ فَأَكۡرَمَهُۥ وَنَعَّمَهُۥ فَيَقُولُ رَبِّيٓ أَكۡرَمَنِ
١٥ وَأَمَّآ إِذَا مَا ٱبۡتَلَىٰهُ فَقَدَرَ عَلَيۡهِ رِزۡقَهُۥ فَيَقُولُ رَبِّيٓ أَهَٰنَنِ ١٦
كَلَّاۖ بَل لَّا تُكۡرِمُونَ ٱلۡيَتِيمَ ١٧ وَلَا تَحَٰٓضُّونَ عَلَىٰ طَعَامِ
ٱلۡمِسۡكِينِ ١٨ وَتَأۡكُلُونَ ٱلتُّرَاثَ أَكۡلٗا لَّمّٗا ١٩
وَتُحِبُّونَ ٱلۡمَالَ حُبّٗا جَمّٗا ٢٠ كَلَّآ إِذَا دُكَّتِ ٱلۡأَرۡضُ دَكّٗا
دَكّٗا ٢١ وَجَآءَ رَبُّكَ وَٱلۡمَلَكُ صَفّٗا صَفّٗا ٢٢ وَجِاْيٓءَ يَوۡمَئِذِۭ
بِجَهَنَّمَۚ يَوۡمَئِذٖ يَتَذَكَّرُ ٱلۡإِنسَٰنُ وَأَنَّىٰ لَهُ ٱلذِّكۡرَىٰ ٢٣

(imene ili nyumba ya chilango). Pa tsiku limenelo munthu adzakumbukira, koma kukumbuka kumeneko kudzam'thandiza chiyani?

21-23 [Osati moteremu kudayenera kukhala kakhalidwe kanu. Pamene nthaka idzatekeseke ndipo ina ndi kuiswa inzake, ndipo akadzabwera Mbuye wako kuti aweruze pakati pa zolengedwa Zake, uku angero ali m'mizeremizere, ndipo mu tsiku lalikulu limenelo idzabweretsedwa jahena. Tsiku limenelo munthu wokanira adzaganizira ndi kulapa, koma mwamtundu wanji kungamuthandize kuganizira ndi kulapa kumeneku kumachita adapyoza muyeso pa ziwirizi pa dziko lapansi komanso nthawi yake idapita?]

(24) Adzanena kalanga ine! Ndikadatsogoza zabwino pa za moyo wanga uno!

[Adzanena: "Kalanga ine! Ndikadatsogoza pa dziko lapansi mu ntchito zomwe zingandithandize ine Tsiku Lomaliza.]

(25) Motero pa tsikuli, palibe wina adzalange monga momwe Allah adzalangire.

(26) Ndiponso sanganjate aliyense monga kunjata kwa Iye Allah.

25-26 [Ndipo mu tsiku loopsa limenelo, sangathe wina aliyense ndipo sadzatha kuti

يَقُولُ يَٰلَيۡتَنِي قَدَّمۡتُ لِحَيَاتِي ﴿٢٤﴾ فَيَوۡمَئِذٖ لَّا يُعَذِّبُ عَذَابَهُۥٓ أَحَدٞ ﴿٢٥﴾
وَلَا يُوثِقُ وَثَاقَهُۥٓ أَحَدٞ ﴿٢٦﴾ يَٰٓأَيَّتُهَا ٱلنَّفۡسُ ٱلۡمُطۡمَئِنَّةُ ﴿٢٧﴾ ٱرۡجِعِيٓ
إِلَىٰ رَبِّكِ رَاضِيَةٗ مَّرۡضِيَّةٗ ﴿٢٨﴾ فَٱدۡخُلِي فِي عِبَٰدِي ﴿٢٩﴾ وَٱدۡخُلِي جَنَّتِي ﴿٣٠﴾

## سُورَةُ ٱلۡبَلَدِ

ترتيبها ٩٠ — آياتها ٢٠

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

لَآ أُقۡسِمُ بِهَٰذَا ٱلۡبَلَدِ ﴿١﴾ وَأَنتَ حِلُّۢ بِهَٰذَا ٱلۡبَلَدِ ﴿٢﴾ وَوَالِدٖ وَمَا وَلَدَ
﴿٣﴾ لَقَدۡ خَلَقۡنَا ٱلۡإِنسَٰنَ فِي كَبَدٍ ﴿٤﴾ أَيَحۡسَبُ أَن لَّن يَقۡدِرَ عَلَيۡهِ
أَحَدٞ ﴿٥﴾ يَقُولُ أَهۡلَكۡتُ مَالٗا لُّبَدًا ﴿٦﴾ أَيَحۡسَبُ أَن لَّمۡ يَرَهُۥٓ أَحَدٌ
﴿٧﴾ أَلَمۡ نَجۡعَل لَّهُۥ عَيۡنَيۡنِ ﴿٨﴾ وَلِسَانٗا وَشَفَتَيۡنِ ﴿٩﴾ وَهَدَيۡنَٰهُ
ٱلنَّجۡدَيۡنِ ﴿١٠﴾ فَلَا ٱقۡتَحَمَ ٱلۡعَقَبَةَ ﴿١١﴾ وَمَآ أَدۡرَىٰكَ مَا ٱلۡعَقَبَةُ ﴿١٢﴾
فَكُّ رَقَبَةٍ ﴿١٣﴾ أَوۡ إِطۡعَٰمٞ فِي يَوۡمٖ ذِي مَسۡغَبَةٖ ﴿١٤﴾ يَتِيمٗا ذَا مَقۡرَبَةٍ
﴿١٥﴾ أَوۡ مِسۡكِينٗا ذَا مَتۡرَبَةٖ ﴿١٦﴾ ثُمَّ كَانَ مِنَ ٱلَّذِينَ ءَامَنُواْ وَتَوَاصَوۡاْ
بِٱلصَّبۡرِ وَتَوَاصَوۡاْ بِٱلۡمَرۡحَمَةِ ﴿١٧﴾ أُوْلَٰٓئِكَ أَصۡحَٰبُ ٱلۡمَيۡمَنَةِ ﴿١٨﴾ وَٱلَّذِينَ
كَفَرُواْ بِـَٔايَٰتِنَا هُمۡ أَصۡحَٰبُ ٱلۡمَشۡـَٔمَةِ ﴿١٩﴾ عَلَيۡهِمۡ نَارٞ مُّؤۡصَدَةُۢ ﴿٢٠﴾

## سُورَةُ ٱلشَّمۡسِ

ترتيبها ٩١ — آياتها ١٥

alange mofanana ndi chilango cha Allah kwa munthu womunyoza, ndipo sangathe wina aliyense kuti amange monga momwe angamangire Allah ndipo sangafike wina aliyense muyeso umenewo mu zimenezo.]

(27) Ee, iwe mzimu wokhazikika (ndi choona)!

(28) Bwerera ku (chiyanjo) cha Mbuye wako uli wokondwera (ndi zomwe wapatsidwa), ndipo uli woyanjidwa (ndi Allah pa zomwe udatsogoza).

(29) Lowa m'gulu la anthu Anga abwino,

(30) Lowa m'munda Mwanga (m'nyumba ya mtendere wosatha).

27-30 [E, iwe mzimu wodekherera ku kumukumbuka Allah ndi chikhulupiriro mwa Iye, ndi zomwe wakonzera anthu okhulupirira mu mautendere, bwerera kwa Mbuye wako uli wachisangalalo ndi ulemerero wa Allah kwa iwe. Ndipo Allah Subhaanahu ndithudi wasangalala nawe, tero lowa mu gulu la akapolo a Allah olungama ndipo ulowe nao limodzi jannah yanga].

# (90) SUURAT-UL-BALAD

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Ndikulumbirira mzinda uwu (wa Makkah).

(2) Ndipo iwe udzatsikira mu mzindawu mwa ufulu (ndi kuonjezera ulemerero).

(3) Ndiponso ndikulumbirira chobereka ndi choberekedwa (kudzera mwa iwo mtundu wa anthu udasungidwa).

(4) Ndithudi tamulenga munthu m'mavuto (kuyambira chiyambi chake mpaka malekezero a moyo wake).

1-4 [Allah walumbirira mzinda uwu wolemekezekawu womwe ndi Makkah ndipo iwe Mtumiki (SAW) udzakhala mu mzinda wolemekezeka umenewu. Ndiponso walumbirira m'bereki wa anthu onse yemwe ndi Adam (AS) komanso ndi awo amene atuluka kuchokera mwa iye mu ana oberekedwa. Ndithudi tidamulenga munthu mu masautso komanso mavuto a kuvutikana nalo dziko lapansi.]

(5) Kodi (munthu wolengedwa ndi mavutoyu) akuganiza kuti palibe amene angamuthe?

[Kodi akuganiza ndi zomwe wazisonkhanitsa mu za chuma kuti ndithu Allah sangamuthe iyeyo?]

(6) Akunena (monyadira kuti): "Ndaononga chuma chambiri (chifukwa choletsa Chisilamu kufala).

(7) Kodi akuganiza kuti palibe akumuona? (Allah akumuona ndipo adzamulipira).

7-8 [Akunena monyada ndi mokhumbiza: "Ndaononga chuma chambiri. Kodi akuganiza mu chochita chake chimenechi kuti ndithu Allah wamphamvu zonse sakumuona ndiponso sakamuwerengera pa chaching'ono chilichonse komanso chachikulu chilichonse?]

(8) Kodi sitidam'pangire maso awiri (amene akuyang'anira)?

(9) Ndi lirime ndi milomo iwiri (zimene akuyankhulira)?

(10) Tam'longosolera njira ziwiri (yabwino ndi yoipa, ndipo tam'patsa mphamvu yosankhira njira imene akufuna).

8-10 [Kodi sitidam'pangire iyeyu maso awiri amene akuyang'anira, komanso lirime ndi milomo iwiri zomwe amayankhulira, ndipo wamufotokozera iyeyo njira ya zabwino komanso zoipa?]

(11) Kodi walikwera phiri lovutalo (phiri la mavuto lomwe lingakam'fikitse ku jannah)

[Kodi bwanji adakadutsa zovuta za Tsiku Lomaliza kudzera mu kupereka chuma chake kuti apeze mtendere].

(12) Nanga n'chiyani chakudziwitsa za kukwera phiri lovutalo? [Ndi chinthu chanji chakudziwitsa iweyo kodi mavuto a Tsiku Lomaliza ndi ati komanso ndi ziti zingathandize kuti uwadutse?]

(13) Kutero ndiko kupereka ufulu kwa kapolo.

[Kumeneko ndiko kupereka ufulu kwa kapolo wokhulupirira mwa Allah kuchokera ku magoli a ukapolo.]

14 Kapena kuwadyetsa (osowa) pa masiku a njala.
15 Amasiye, achibale (ndi amene sali achibale),
16 Kapena wosauka wafumbi lokhalokha (chifukwa cha kuvutika kwambiri).

14-16 [Kapena kupereka chakudya mu tsiku la njala yoopsa kwa munthu wamasiye wochokera mwa achibale kuti usonkhane mwa iye ubwino wa sadaka ndi kulumikiza ubale kapena wosauka,wosowa amene alibiretu kanthu kalikonse].

17 Kenako iye n'kukhala m'modzi mwa okhulupirira amene akulangizana za kupirira, ndiponso za chifundo.

[Kenako, pamodzi ndi zimene zatchulidwazi mu ntchito zabwino, nakhala mu gulu la anthu amene ayeretsa chikhulupiriro mwa Allah komanso namalangizana wina ndi mnzake za kupirira pa kumvera Allah ndi kusiya kumuchimwira komanso akulangizana za zochitira chifundo zolengedwa].

18 Otero ndiwo (anthu abwino) a ku dzanja la manja. [Amene achita zinthu zimenezi ndi eni aku dzanjadzanja, amene adzatengedwe iwowo Tsiku la Kiyama mbali ya kumanja kunka ku jannah].

19 Koma amene sadakhulupirire Ayah Zathu ndi anthu aku dzanja lamanzere (oipa).

[Ndipo anthu okanira Qur'aan iwowo ndi anthu amene adzatengedwa Tsiku la Kiyama ku mbali ya ku manzere kunka nawo ku moto].

20 Moto wozungulira mabali zonse udzakhala pa iwo (ndi kuwatsekera makomo).[Malipiro awo ndi jahena yotsekedwa makomo ake pa iwo.]

## (91) SUURAT-S'HAMS

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Ndikulumbirira dzuwa ndi dangalira lake.
2 Ndi mwezi pamene ukulitsatira dzuwalo (ndi kulowa m'malo mwake powalitsa litalowa).
3 Ndi masana pamene ukulisonyeza poyera (kuti lisaphimbidwe).
4 Ndi usiku pamene ukuliphimba.
5 Ndi thambo ndi (mwini mphamvu zonse Wamkulu) Yemwe adalimanga ndi kulitukula.
6 Ndi nthaka ndi (Mwini mphamvu zonse wamkulu) Yemwe adaiyala (mbali zonse ndikuichita kukhala ngati choyala).
7 Ndi mzimu ndi yemwe adauyambitsa ndi kuwulinganiza (poupatsa mphamvu).
8 Ndipo adaudziwitsa zoipa zake ndi zabwino zake (ndi kuwupatsa ufulu ndi mphamvu zochitira zimene ukufuna).
9 Ndithu , wapambana amene wauyeretsa (ndi mapemphero ndi kuchita zabwino).
10 Ndipo ndithu, wataika amene wauononga pobisa ulemerero wake ndi kuupha (kuti usakonzekere kuchita zabwino)

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَٰنِ الرَّحِيمِ

وَالشَّمْسِ وَضُحَاهَا ﴿١﴾ وَالْقَمَرِ إِذَا تَلَاهَا ﴿٢﴾ وَالنَّهَارِ إِذَا جَلَّاهَا ﴿٣﴾
وَاللَّيْلِ إِذَا يَغْشَاهَا ﴿٤﴾ وَالسَّمَاءِ وَمَا بَنَاهَا ﴿٥﴾ وَالْأَرْضِ وَمَا طَحَاهَا
﴿٦﴾ وَنَفْسٍ وَمَا سَوَّاهَا ﴿٧﴾ فَأَلْهَمَهَا فُجُورَهَا وَتَقْوَاهَا ﴿٨﴾ قَدْ
أَفْلَحَ مَنْ زَكَّاهَا ﴿٩﴾ وَقَدْ خَابَ مَنْ دَسَّاهَا ﴿١٠﴾ كَذَّبَتْ ثَمُودُ
بِطَغْوَاهَا ﴿١١﴾ إِذِ انْبَعَثَ أَشْقَاهَا ﴿١٢﴾ فَقَالَ لَهُمْ رَسُولُ اللَّهِ
نَاقَةَ اللَّهِ وَسُقْيَاهَا ﴿١٣﴾ فَكَذَّبُوهُ فَعَقَرُوهَا فَدَمْدَمَ
عَلَيْهِمْ رَبُّهُمْ بِذَنْبِهِمْ فَسَوَّاهَا ﴿١٤﴾ وَلَا يَخَافُ عُقْبَاهَا ﴿١٥﴾

### سُورَةُ اللَّيْلِ

آياتها ٢١ — ترتيبها ٩٢

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَٰنِ الرَّحِيمِ

وَاللَّيْلِ إِذَا يَغْشَىٰ ﴿١﴾ وَالنَّهَارِ إِذَا تَجَلَّىٰ ﴿٢﴾ وَمَا خَلَقَ الذَّكَرَ وَالْأُنْثَىٰ ﴿٣﴾
إِنَّ سَعْيَكُمْ لَشَتَّىٰ ﴿٤﴾ فَأَمَّا مَنْ أَعْطَىٰ وَاتَّقَىٰ ﴿٥﴾ وَصَدَّقَ بِالْحُسْنَىٰ ﴿٦﴾
فَسَنُيَسِّرُهُ لِلْيُسْرَىٰ ﴿٧﴾ وَأَمَّا مَنْ بَخِلَ وَاسْتَغْنَىٰ ﴿٨﴾ وَكَذَّبَ بِالْحُسْنَىٰ
﴿٩﴾ فَسَنُيَسِّرُهُ لِلْعُسْرَىٰ ﴿١٠﴾ وَمَا يُغْنِي عَنْهُ مَالُهُ إِذَا تَرَدَّىٰ ﴿١١﴾ إِنَّ عَلَيْنَا
لَلْهُدَىٰ ﴿١٢﴾ وَإِنَّ لَنَا لَلْآخِرَةَ وَالْأُولَىٰ ﴿١٣﴾ فَأَنْذَرْتُكُمْ نَارًا تَلَظَّىٰ ﴿١٤﴾

1-10 [Allah walilumbirira dzuwa ndi masana ake komanso ndi kutuluka kwake m'mawa. Komanso walumbirira mwezi ukalitsatira dzuwalo potuluka ndi polowa. Walumbiriranso usana ukaonekera ndi kuchotsa mdima. Komanso walumbirira usiku pamene umaphimba nthaka ndi kukhala zomwe zili pamenepo za mdima. Walumbiriranso thambo ndi kamangidwe kake kaluntha. Komanso walumbirira nthaka ndi kutambasuka kwake ndinso walumbirira mzimu uliwonse ndi kukwaniritsa kwa Allah pa kuwulenga kuti udzichita nchito zofunikira zake naulongosolera njira ya choipa komanso ya chabwino. Ndithudi wapambana amene wauyeretsa ndi kuumeretsa komanso kuukuza ndi zabwino. Ndithudi wataika amene waubisa mzimu wake mu machimo.]

11 Asamudu adakanira (mneneri wawo) chifukwa cha kulumpha malire kwawo.
12 Pamene woipitsitsa wawo adadzipereka (kupha ngamira yozizwitsa).
13 (pamenepo Swaaleh (AS) yemwe adali) Mtumiki wa Allah adawauza "Isiyeni ngamira ya Allah (idye m'dziko la Allah) musailetse kumwa madzi (pa tsiku lake)".

14 Koma adamutsutsa (Mtumiki Swaaleh AS) ndi kuipha (ngamira ija) kwa chifukwa chimenecho Mbuye wawo (Allah) adawaononga chifukwa cha tchimo lawo adangowafafaniza (onse mu nthaka).
15 Iye saopa zotsatira za chilangochi (chifukwa amenewo ndi malipiro a chilungamo pa zomwe adachita).
11-15 [Asamudu adamukanira mneneri wake pofika kwawo mapeto mu kunyozera, pamene adadzambatuka yemwe ali wochulukitsa mu mtunduwo kuipitsitsa kukapha ngamira ija. Ndipo Mtumuki wa Allah Swaleh (AS) adauza kuti: "Pewani kuikhudza ngamira ndi choipa ndithu imeneyi ndi chozizwitsa chomwe Allah wachitumiza kwa inu chosonyeza kuona kwa mneneri wanu. Ndipo pewani kuputa pa chakumwa chake ndithu ili nalo tsiku lakumwa ngamirayi komanso nanunso muli nalo tsiku lodziwika lakumwa. Ndiye zidawalemera iwowo zimenezo kotero adam'tsutsa mu zomwe adawaopseza nazo tero adaipha. Mbuye wawo ndiye adawavindikira ndi chilango chifukwa cha tchimo lawolo. Ndiye adachichita chilangocho pa iwo mofanana onse moti palibe mwa iwo ndi m'modzi yemwe amene adapulumuka. Ndipo Iye Amene kuthekera Kwake nkofalikira ponseponse saopa zotsatira za zomwe adawatsitsira iwowo mu chilango chowawitsachi].

## (92) SUURAT ALLAHIL

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Ndikulumbirira usiku pamene ukuphimba (chilichonse).
2 Ndi masana pamene kukuyera,
3 Ndiponso yemwe adalenga chachimuna ndi chachikazi.
4 Ndithu zochita zanu n'zosiyanasiyana (zina n'zokhazikika pabwino kwa ozichitayo, pomwe zina ndi zomuika mmavuto).
1-4 [Allah Subhaanahu walumbirira usiku pamene ukuphimba ndi mdima wake nthaka ndi zomwe zili pamenepo. Komanso ndi masana akaonekera ku mdima wa usiku ndi kuwala kwake. Walumbiriranso kulenga kwa zinthu ziwiriziwiri chachimuna ndi chachikazi. Ndithudi ntchito zanu ndi zosiyanasiyana pakati panu ndi wogwirira ntchitoyo chifukwa cha dziko lapansi, ndi wogwirira ntchitoyo chifukwa cha Tsiku Lomaliza.]
5 Tsono yemwe akupereka (pa njira ya Allah) ndi kumamuopa (Mbuye wake ndi kupewa zoletsedwa).
6 Ndi kumavomereza chinthu chabwino (komwe kuli kukhulupirira Allah mwanzeru).
7 Timufewetsera (njira) yopita ku zabwino.
5-7 [ Tsono amene wapereka kuchokera mu chuma chake ndi kumuopa Allah mu zimenezo navomereza zoti "palibe wopembedzedwa mwa choonadi kupatula Allah" ndi zomwe liwu limeneli lasonyeza komanso zimene zatsatira pamenepa mu malipiro, ndiye timuongolera komanso kumupatsa kuthekera ku njira za zabwino ndi kulungama ndiponso timufewetsera iyeyo zinthu zake zonse].
8 Koma uyo achite umbombo ndi kuganiza za kuti iye payekha ngokwana.
9 Ndi kumatsutsa chinthu chabwino.
10 Timufewetsera (njira) yom'pititsira ku mavuto (a muyaya).
11 Chuma chake sichidzam'thandiza (chilichonse) akadzagwera (ku moto).
8-11 [Tsono amene wachita umbombo ndi chuma chake nadzikwaniritsa ku malipiro a Mbuye wake nakanira zoti "palibe wina wopembedzedwa mwa choonadi kupatula Allah" ndi zomwe liwuli lasonyeza komanso zimene zatsatira pamenepa mu malipiro ndiye kuti timufewetsera njira za kuipa. Ndipo sichidzam'thandiza iye chuma chake chimene adachitira umbombo pamene akadzagwera mu moto.]
12 Ndithu Ife ndi Amene timalongosolera (anthu) njira yabwino.
13 Ndipo ndithu, moyo womaliza ndi moyo woyamba uli m'manja Mwathu (timam'patsa amene tam'funa).
12-13 [Ndithu nkoyenera kwa Ife mu ubwino Wathu komanso luntha Lathu kuti tifotokozere njira ya chiongoko yofikitsa kwa Allah ndi jannah Yake ku njira ya chisokero. Ndipo tili nawo Ife umwini wa moyo wa Tsiku Lomaliza ndi umoyo wa dziko lapansi.
14 Basi, ndikukuchenjezani za moto woyaka mwamphamvu. [Ndiyetu ndakuchenjezani inu anthu komanso ndakuopsezani moto woyaka umene uli moto wa jahena.
15 Palibe amene akaulowe koma (kafiri) woipitsitsa kwambiri.
16 Yemwe amakanira (choona) ndi kunyoza (zisonyezo za Allah).
15-16 [Sakaulowa moto umenewo kupatula munthu amene ali woipitsitsa kwambiri amene adakanira Mneneri wa Allah Muhammad (SAW) nanyozera chikhulupiriro mwa Allah ndi Mtumiki Wake (SAW) ndi kuwamvera awiriwa.]
17 Koma yemwe akuopa Allah kwambiri akaikidwa kutali ndi moto.
18 Amene akupereka chuma chake (mu njira zabwino) ndi cholinga chodziyeretsa (ku uve wa umbombo).
19 Ndipo palibe aliyense kwa iye amene adam'chitira zachifundo zomwe zikulipidwa.

(20) Koma (akuchita zimenezi) pofuna chikondi cha Mbuye wake Wapamwambamwamba.
(21) Ndipo posachedwa adzasangalala (adzapeza) mokwanira ndi mokondweretsedwa (kwa Mbuye wake zomwe ankazifuna).

17-21 [Ndipo adzapewetsedwa ku motowo munthu amene ali woopa kwambiri, amene amapereka chuma chake chifukwa chofuna kuonjezera mu zabwino. Kupereka kwa chuma kwakeko sikubwezera chabwino kwa munthu amene wamuchitira iyeyu chabwino ayi koma ndithu iyeyu akufuna ndi zimenezo nkhope ya Mbuye wake Wapamwambamwamba ndi chiyanjo Chake. Ndipo adzamupatsa Allah mu jannah zomwe adzasangalale nazo.]

## (93) SUURAT ADHUHAA

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Ndikulumbirira masana dzuwa litakwera (imene ili nthawi ya ntchito).
(2) Ndi usiku pamene ukuvindikira (mdima).
(3) Sadakusiye Mbuye wako (iwe Muhammad SAW) ndiponso sadakude.

1-3 [Allah walumbirira nthawi ya kum'mawa ndipo cholinga chake, ndi masana onse. Ndiponso walumbirira usiku ukakhazikika ndi zolengedwa ndi kulimbikira mdima wake. Ndiponso amalumbirira Allah zimene wazifuna mu zolengedwa Zake, tsono cholengedwa ndi kosavomerezeka kwa chimenecho kulumbirira wina aliyense wosakhala Mlengi wake, ndithudi kulumbirira zina zake zosakhala Allah ndi shirk. Sadakusiye iwe Mneneri (SAW) Mbuye wako komanso sadakude pokuchedwetsera wahyu kwa iwe.

(4) Ndithu, umoyo wa tsiku lili nkudza ndi wabwino kwa iwe kuposa umoyo woyambawu.
(5) Ndipo ndithu posachedwapa akupatsa Mbuye wako (zabwino za m'dziko lapansi ndi Tsiku Lomaliza) ndipo ukondwera.

4-5 [Ndithudi nyumba ya Tsiku Lomaliza ndiyabwino kwa iwe kuposa nyumba ya dziko lapansi ndipo ndithu adzakupatsa Mbuye wako iwe Mneneri (SAW) mu mitundu ya mautendere mu Tsiku Lomaliza kotero udzasangalala nazo.

(6) Kodi sadakupeze uli wamasiye ndipo adakupatsa pokhala pabwino?
(7) Ndipo adakupeza uli wosazindikira (Qur'aan) nakuongola (Pokuzindikiritsa Qur'aaniyo ndi malamulo a chipembedzo).
(8) Ndiponso adakupeza uli wosauka nakulemeretsa?

6-8 [kodi sadakupeze kale uli wamasiye nakusamalira ndi kukulera? Ndiponso kodi sadakupeze uli wosadziwa kuti Buku ndi chiyani ngakhalenso kuti chikhulupiriro

لَا يَصۡلَىٰهَآ إِلَّا ٱلۡأَشۡقَى ﴿١٥﴾ ٱلَّذِي كَذَّبَ وَتَوَلَّىٰ ﴿١٦﴾ وَسَيُجَنَّبُهَا
ٱلۡأَتۡقَى ﴿١٧﴾ ٱلَّذِي يُؤۡتِي مَالَهُۥ يَتَزَكَّىٰ ﴿١٨﴾ وَمَا لِأَحَدٍ عِندَهُۥ مِن
نِّعۡمَةٖ تُجۡزَىٰٓ ﴿١٩﴾ إِلَّا ٱبۡتِغَآءَ وَجۡهِ رَبِّهِ ٱلۡأَعۡلَىٰ ﴿٢٠﴾ وَلَسَوۡفَ يَرۡضَىٰ ﴿٢١﴾

ترتيبها ٩٣ — سُورَةُ الضُّحَىٰ — آياتها ١١

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

وَٱلضُّحَىٰ ﴿١﴾ وَٱلَّيۡلِ إِذَا سَجَىٰ ﴿٢﴾ مَا وَدَّعَكَ رَبُّكَ وَمَا قَلَىٰ ﴿٣﴾
وَلَلۡأٓخِرَةُ خَيۡرٞ لَّكَ مِنَ ٱلۡأُولَىٰ ﴿٤﴾ وَلَسَوۡفَ يُعۡطِيكَ رَبُّكَ
فَتَرۡضَىٰٓ ﴿٥﴾ أَلَمۡ يَجِدۡكَ يَتِيمٗا فَـَٔاوَىٰ ﴿٦﴾ وَوَجَدَكَ ضَآلّٗا
فَهَدَىٰ ﴿٧﴾ وَوَجَدَكَ عَآئِلٗا فَأَغۡنَىٰ ﴿٨﴾ فَأَمَّا ٱلۡيَتِيمَ فَلَا تَقۡهَرۡ
﴿٩﴾ وَأَمَّا ٱلسَّآئِلَ فَلَا تَنۡهَرۡ ﴿١٠﴾ وَأَمَّا بِنِعۡمَةِ رَبِّكَ فَحَدِّثۡ ﴿١١﴾

ترتيبها ٩٤ — سُورَةُ الشَّرۡحِ — آياتها ٨

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

أَلَمۡ نَشۡرَحۡ لَكَ صَدۡرَكَ ﴿١﴾ وَوَضَعۡنَا عَنكَ وِزۡرَكَ ﴿٢﴾ ٱلَّذِيٓ
أَنقَضَ ظَهۡرَكَ ﴿٣﴾ وَرَفَعۡنَا لَكَ ذِكۡرَكَ ﴿٤﴾ فَإِنَّ مَعَ ٱلۡعُسۡرِ يُسۡرًا ﴿٥﴾ إِنَّ
مَعَ ٱلۡعُسۡرِ يُسۡرٗا ﴿٦﴾ فَإِذَا فَرَغۡتَ فَٱنصَبۡ ﴿٧﴾ وَإِلَىٰ رَبِّكَ فَٱرۡغَب ﴿٨﴾

n'chiyani nakuphunzitsa zomwe siudali kuzidziwa nakudalitsa ku ntchto zabwino? Komanso kodi sadakupeze uli wosowa nakusakira iwe riziq lako ndipo naulemeretsa mtima wako pokhutira ndi kupirira?]

(9) Basi, wamasiye usamuvutitse.
(10) Ndiponso wopempha usamukalipire.
(11) Tsono mtendere wa Mbuye wako uwutchule (pothokoza ndi kugwira ntchito zabwino)

9-11 [Tsono wamasiye usamuipitsire kukhalirana naye kwake, ndipo wopempha usamukalipire koma umudyetse ndi kum'pangira zofunikira zake. Tsono za mtenedere wa Mbuye wako womwe waukwaniritsa pa iwe, khala woutchula.

## (94) SUURAT AS'SHARH

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Kodi sitidachiphanule chifuwa chako (pokupatsa chiongoko ndi chikhulupiriro ndi nzeru zambiri)?
(2) Ndipo takuchotsera mtolo wako.
(3) Mtolo umene udalemeretsa msana wako?
(4) Ndipo takukweza kutchulidwa kwako.

1-4[Kodi sitidakutambasulire iwe Mneneri (SAW) chifuwa chako ndi malamulo a chipembedzo

سُورَةُ التِّينِ — ترتيبها ٩٥ — آياتها ٨

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَٰنِ الرَّحِيمِ

وَالتِّينِ وَالزَّيْتُونِ ﴿١﴾ وَطُورِ سِينِينَ ﴿٢﴾ وَهَٰذَا الْبَلَدِ الْأَمِينِ ﴿٣﴾
لَقَدْ خَلَقْنَا الْإِنسَانَ فِي أَحْسَنِ تَقْوِيمٍ ﴿٤﴾ ثُمَّ رَدَدْنَاهُ أَسْفَلَ سَافِلِينَ
﴿٥﴾ إِلَّا الَّذِينَ آمَنُوا وَعَمِلُوا الصَّالِحَاتِ فَلَهُمْ أَجْرٌ غَيْرُ مَمْنُونٍ ﴿٦﴾
فَمَا يُكَذِّبُكَ بَعْدُ بِالدِّينِ ﴿٧﴾ أَلَيْسَ اللَّهُ بِأَحْكَمِ الْحَاكِمِينَ ﴿٨﴾

سُورَةُ الْعَلَقِ — ترتيبها ٩٦ — آياتها ١٩

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَٰنِ الرَّحِيمِ

اقْرَأْ بِاسْمِ رَبِّكَ الَّذِي خَلَقَ ﴿١﴾ خَلَقَ الْإِنسَانَ مِنْ عَلَقٍ ﴿٢﴾ اقْرَأْ وَرَبُّكَ
الْأَكْرَمُ ﴿٣﴾ الَّذِي عَلَّمَ بِالْقَلَمِ ﴿٤﴾ عَلَّمَ الْإِنسَانَ مَا لَمْ يَعْلَمْ ﴿٥﴾ كَلَّا إِنَّ
الْإِنسَانَ لَيَطْغَىٰ ﴿٦﴾ أَن رَّآهُ اسْتَغْنَىٰ ﴿٧﴾ إِنَّ إِلَىٰ رَبِّكَ الرُّجْعَىٰ ﴿٨﴾ أَرَأَيْتَ
الَّذِي يَنْهَىٰ ﴿٩﴾ عَبْدًا إِذَا صَلَّىٰ ﴿١٠﴾ أَرَأَيْتَ إِن كَانَ عَلَى الْهُدَىٰ ﴿١١﴾ أَوْ أَمَرَ
بِالتَّقْوَىٰ ﴿١٢﴾ أَرَأَيْتَ إِن كَذَّبَ وَتَوَلَّىٰ ﴿١٣﴾ أَلَمْ يَعْلَم بِأَنَّ اللَّهَ يَرَىٰ ﴿١٤﴾ كَلَّا لَئِن
لَّمْ يَنتَهِ لَنَسْفَعًا بِالنَّاصِيَةِ ﴿١٥﴾ نَاصِيَةٍ كَاذِبَةٍ خَاطِئَةٍ ﴿١٦﴾ فَلْيَدْعُ نَادِيَهُ
﴿١٧﴾ سَنَدْعُ الزَّبَانِيَةَ ﴿١٨﴾ كَلَّا لَا تُطِعْهُ وَاسْجُدْ وَاقْتَرِب ۩ ﴿١٩﴾

ndi kuitanira kwa Allah komanso ndi kukhala ndi mbiri ya makhalidwe abwino, ndipo tachotsa ndi zimenezo mtolo wako umene umalemeretsa msana wako. Ndipo takuchita iweyo ndi zomwe takudalitsa nazo mu zaulemerero kukhala pa sitepe yapamwambamwamba?

5 Ndithu pali chovuta palinso zabwino zambiri.

6 Ndithu, pali chovuta pali zabwino zambiri.

5-6 [Ndipo asakupotoze masautso a adani kusiya kufalitsa uthenga, popeza kuti ndithudi pali mavuto, pali mtendere, ndithudi pamodzi ndi mavuto pali mtendere.]

7 Basi ukamaliza ntchito ( yolalikira ndi jihad) limbikira kupemphera.

8 Ndipo khala wolakalaka (zabwino zomwe zili) kwa Mbuye wako.

7-8 [Ukamaliza mu zinthu za dziko lapansi ndi ntchito zake, limbikira pochita ibaadah. Komanso kwa Mbuye wako Yekhayo khala wolakalakalira zomwe zili kwa Iye]

## (95) SUURAT-TTIIN

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Ndikulumbirira mitengo ya tiini ndi zaytuuni (pansi pa mitengo imeneyi Ibrahim ndi Nuh (AS) adalandira uneneri).

2 Ndi phiri la Sinai (pamene Allah adamulankhulira Mussa (AS).

3 Ndiponso mzinda uwu (wolemekezeka) wa mtendere (Makka momwe adapatsidwira uneneri Muhammad SAW).

4 Palibe chikaiko, tamulenga munthu m'kalengedwe kabwino, kolingana (ndipo ali ndi mbiri zabwino).

5 Pambuyo pake tamubwezera pansi kuposa wa pansi (chifukwa cha kusatsatira zimene tidamulengera).

6 Kupatula amene akhulupirira ndi kumachita zabwino, adzakhala nawo malipiro osatha.

1-6 [Allah walumbirira tiini ndi zaituuni yomwe ili m'magulu a zipatso zotchuka. Komanso walumbirira phiri la Tuur Siinaai lomwe Allah adamulankhula Mussa (AS) pamwamba pake kumuyankhulitsa. Komanso walumbirira mzinda uwu wabata ku mantha aliwonse womwe ndi mzinda wa Makka –malo amene Chisilamu chinatsikira. Ndithudi tidamulenga munthu mumaonekedwe abwino koposa kenako timamubwezeretsa ku moto akapanda kumvera Allah ndi kutsatira Atumiki, koma anthu amene adakhulupirira ndi kugwira ntchito zolungama ali nawo malipiro akulu osadukiza komanso osapunguka.]

7 Basi, ndi chiyani chakuchititsa kuti ukanire kuuka ndi malipiro pambuyo (poona mphamvu Zathu pa chilichonse?)

[Ndi chinthu chanji chakuchititsa iwe munthu kuti ukanire za kuuka kwa akufa ndi malipiro chonsecho maumboni ali poyera a kuthekera kwa Allah pa zimenezo?]

8 Kodi Allah (Amene adachita zomwe takuuzanizi) si Muweruzi wa nzeru kuposa aweruzi onse (popanga ndi polinganiza).

[Kodi sali Allah Amene adalichita tsiku limeneli logamula pakati pa anthu ndi Wanzeru zakuya kuposa wina aliyense mu zonse zimene adalenga? Indedi! Kodi nkutheka kusiidwa zolengedwa popanda kalikonse popanda kulamulidwa kapena kuletsedwa, kapena kulipidwa ngakhalenso kulangidwa? Zimenezo sizingakhale zoona komanso sizingachitike.]

## (96) SUURA-UL-ALAQ

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Werenga! (Iwe Muhammad SAW zomwe ukuvumbulutsidwa) m'dzina la Mbuye wako Yemwe adalenga (zolengedwa zonse).

2 Adalenga munthu (wokwanira,wathupi lake, wanzeru zake) ndi dontho la magazi.

3 Werenga! Ndipo Mbuye wako ndi Mfulu,
4 Yemwe waphunzitsa (munthu kulemba) ndi cholembera.
5 Waphunzitsa munthu zinthu (zambiri) zomwe (iye) sadali kuzidziwa (ndiponso sadali kuganizira kuti angazidziwe).

1-5 [Werenga iwe Mneneri (SAW) zomwe zavumbulutsidwa kwa iwe za mu Qur'aan potsegulira ndi dzina la Mbuye wako Yemwe mwayekhayekha ali nako kulenga. Yemwe adalenga munthu aliyense kuchokera ku kachidutswa ka magazi okhathamira ofiira. Werenga iwe Mneneri (SAW) zomwe zavumbulutsidwa kwa iwe ndipo ndithu Mbuye wako ndi Wochuluka ubwino, Wopatsa kwambiri, Yemwe adaphunzitsa zolengedwa Zake kulemba ndi cholembera. Adaphunzitsa munthu zinthu zomwe sadali kuzidziwa, komanso adamuchotsa kuchokera ku mdima wa umbuli kunka naye ku dangalira la kuzindikira.]

6 Zoona ndithu, koma munthu akupyola malire (podzikweza ndi Allah wake).
7 Chifukwa chodziona kuti walemera.
8 Palibe chikaiko,(iwe Muhammad) kobwerera (onse) nkwa Mbuye wako basi (adzawaukitsa).

6-8 [Zoonadi ndithu munthu akupyola malire a Allah kukumunyaditsa kulemera. Ayenera kudziwa aliyense wopyola malire kuti ndithu kobwerera n'kwa Allah kotero kuti adzamulipira munthu aliyense ndi ntchito zake.]

9 Kodi wamuona yemwe akuletsa,
10 Kapolo (wa Allah) akamafuna kupemphera?
11 Tandiuza ngati ali pa chiongoko.
12 Kapena kuti akulamulira zoopa Allah.
13 Tandiuza (za woletsayo) ngati akutsutsa (zimene wadza nazo Mneneri SAW) ndi kunyoza (chikhulupiriro ndi ntchito yabwino)?
14 Kodi sakudziwa kuti Allah akuona (machitidwe ake. Ndipo adzam'lipira)?
15 Ayi ndithu, ngati sasiya timukoka tsitsi la pa liwombo (tiligwira mwamphamvu liwombo lake ndikukaliponya ku moto pamodzi ndi iye mwini).
16 Liwombo labodza ndiponso lamachimo.
17 Basi aliitane gulu lakelo (la amene amakhala nawo pa bwalo kuti am'thandize pano pa dziko kapena Tsiku Lomaliza).
18 Nafe tiitana Azzabaaniya (angero a ku moto kuti am'pulumutse Muhammad SAW ndi om'tsatira ake ndikutinso amponye woletsayo ndi anzakewo ku moto).
19 Ayi ndithu (asiye zimenezi), usamumvere (pa zimene akukuletsazo pitiriza kupemphera kwako) ndi kugwetsa nkhope yako. Dziyandikitse ndi zimenezo (kwa Mbuye wako).

11-19 [Kodi waona zodabwitsa koposa kupyola malire kwa munthu ameneyu (amene ali Abuu Jahli) amene akuletsa kapolo wa Ife akamapemphera (amene ali Muhammad SAW)? Kodi ukuwona bwanji ngati uyu woletsedwayu kupemphera ali pa chiongoko,ndiye motani akumuletsa? Kapena ngati ali wolamulira ena zomuopa Allah, kodi angamuletsebe zimenezo? Ukuona bwanji ngati atakanira uyu woletsayu zomwe akuitanidwira ku zimenezo ndipo iye ndi kuzinyozera, kodi sakudziwa kuti ndithu Allah akuona zonse zimene akuchita? Zinthu sizili ngati m'mene akuganizira Abuu Jahli. Akapanda kubwerera ameneyu ku chilekanitso chakechi ndi masautso akewa ndithudi tidzamugwira tsogolo la mutu wake kumugwira kwa nkhanza ndi kuponyedwa ku moto. Liwombo lakelo ndi liwombo labodza mu zoyankhula zake, lolakwa mu zochita zake. Abweretse wopyola malire ameneyu anthu a pa bwalo lake amene angawapemphe chipulumutso ndi iwo, Ife tidzaitana angero achilango. Zinthu sizili monga akuganizira Abuujahli, ndithu iyeyu sadzakupweteketsa iwe Mtumiki (SAW) ndi choipa chilichonse tero usamumvere mu zomwe akukuitanira iweyo zosiya swalaat, m'malo mwake lambira chifukwa cha Mbuye wako ndipo dziyandikitse kwa Iye podzikondetsetsa kwa Iye kudzera mu kumumvera.]

## (97) SUURAT-UL –QADRI

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Ndithu taivumbulutsa (Qur'aan) mu usiku wa Lailatul Qadri (usiku wolemekezeka).

[Ndithu Ife taivumbulutsa Qur'aan mu usiku wolemekezeka ndi waubwino, umenewu ndi usiku umodzi m'mausiku a mwezi wa Ramadhan.]

2 Ndi chiyani chingakudziwitse usiku wolemekezekawu? [Ndipo ndi chiyani chingakudziwitse iwe Mneneri kodi usiku wa Lailatul Qadri ndi ulemerero ndi chiyani?]

3 (Kum'pembedza Allah mu) usiku umenewo kuli kwabwino kuposa (kum'pembedza) m'miyezi chikwi chimodzi (1,000) momwe mulibe Lailatul Qadri.

[Usiku wa Lailatul Qadri ndi usiku wa mwayi, ubwino wake ngoposa miyezi chikwi chimodzi (1,000) yomwe mulibe Lailatul Qadri].

4 Amatsika angero ndi Jibril (AS) m'menemo potsatira lamulo la Allah kudzalongosola chinthu chilichonse. [Kumachuluka kutsika kwa angero ndi Jibril mu usiku umenewo ndi lamulo la Mbuye wawo kuchokera ku lamulo lililonse limene walilinganiza mu chaka chimenecho.]

5 Mtendere! (Usiku umenewo, palibe mavuto ndi zoipa) mpakana m'bandakucha.

## سُورَةُ القَدْرِ

ترتيبها ٩٧ — آياتها ٥

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَٰنِ الرَّحِيمِ

إِنَّا أَنزَلْنَٰهُ فِي لَيْلَةِ الْقَدْرِ ﴿١﴾ وَمَا أَدْرَىٰكَ مَا لَيْلَةُ الْقَدْرِ ﴿٢﴾
لَيْلَةُ الْقَدْرِ خَيْرٌ مِّنْ أَلْفِ شَهْرٍ ﴿٣﴾ تَنَزَّلُ الْمَلَٰٓئِكَةُ وَالرُّوحُ
فِيهَا بِإِذْنِ رَبِّهِم مِّن كُلِّ أَمْرٍ ﴿٤﴾ سَلَٰمٌ هِيَ حَتَّىٰ مَطْلَعِ الْفَجْرِ ﴿٥﴾

## سُورَةُ البَيِّنَةِ

ترتيبها ٩٨ — آياتها ٨

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَٰنِ الرَّحِيمِ

لَمْ يَكُنِ الَّذِينَ كَفَرُوا مِنْ أَهْلِ الْكِتَٰبِ وَالْمُشْرِكِينَ مُنفَكِّينَ
حَتَّىٰ تَأْتِيَهُمُ الْبَيِّنَةُ ﴿١﴾ رَسُولٌ مِّنَ اللَّهِ يَتْلُوا صُحُفًا مُّطَهَّرَةً ﴿٢﴾
فِيهَا كُتُبٌ قَيِّمَةٌ ﴿٣﴾ وَمَا تَفَرَّقَ الَّذِينَ أُوتُوا الْكِتَٰبَ إِلَّا مِنۢ
بَعْدِ مَا جَآءَتْهُمُ الْبَيِّنَةُ ﴿٤﴾ وَمَآ أُمِرُوٓا إِلَّا لِيَعْبُدُوا اللَّهَ مُخْلِصِينَ
لَهُ الدِّينَ حُنَفَآءَ وَيُقِيمُوا الصَّلَوٰةَ وَيُؤْتُوا الزَّكَوٰةَ ۚ وَذَٰلِكَ دِينُ
الْقَيِّمَةِ ﴿٥﴾ إِنَّ الَّذِينَ كَفَرُوا مِنْ أَهْلِ الْكِتَٰبِ وَالْمُشْرِكِينَ
فِي نَارِ جَهَنَّمَ خَٰلِدِينَ فِيهَآ ۚ أُولَٰٓئِكَ هُمْ شَرُّ الْبَرِيَّةِ ﴿٦﴾ إِنَّ
الَّذِينَ ءَامَنُوا وَعَمِلُوا الصَّٰلِحَٰتِ أُولَٰٓئِكَ هُمْ خَيْرُ الْبَرِيَّةِ ﴿٧﴾

[Usiku umenewu ndi mtendere wokhawokha mopandamo choipa m'menemo kufikira kutuluka kwa m'bandakucha].

## (98) SUURAT-UL- BAYYINAT

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Amene adakanira (Allah ndi Mtumiki Wake SAW) mwa amene adapatsidwa Buku ndi amushrikina sadali olekana (ndi umbuli wawo ndi kusalabadira kwawo choona) mpaka pomwe chidawadzera chisonyezo choonekera poyera.

[Sadali anthu okanira ochokera mwa Ayuda ndi Akhristu komanso opembedza mafano kuti nkusiya ukafiri wawo kufikira chitawafikira chizindikiro chimene adalonjezedwa nacho m'Mabuku amene adatsogola].

(2) (Yemwe ndi) Mtumiki (SAW) wochokera kwa Allah akuwawerengera makalata oyeretsedwa (ku zonama). [Ameneyu ndi Mtumiki wa Allah Muhammad (SAW) amene akuwawerengera Qur'an m'makalata oyeretsedwa.]

(3) Omwe mkati mwake muli malamulo owongoka (ofotokoza za choona).

[Mu makalata m'menemo muli nkhani zoona ndi malamulo achilungamo omwe akuongolera ku choonadi ndi njira yoongoka.]

(4) Sadalekane omwe adapatsidwa mabuku mpakana pomwe chidawafikira chisonyezo (chosonyeza kuti Muhammad SAW ndi Mtumiki wa Allah yemwe adalonjezedwa m'mabuku awo.]

[Ndipo sadalekane anthu amene adapatsidwa Buku mwa Ayuda ndi Akhristu mu kukhala koti Muhammad (SAW) ndi mtumiki mwachoonadi chifukwa cha zomwe akumazipeza mu mbiri zake mu Buku lawo kupatula pamene adatsimikiza kuti ndithu iyeyudi ndi mneneri amene adalonjezedwa naye mu Taurat ndi Injiil, ndipo adali ogwirizana pa zakuona kwa uneneri wake, koma pamene adatumizidwa, adaukanira utumikiwo komanso adasiyana.]

(5) Sadalamulidwe (china) koma kuti am'pembedze Allah (M'modzi Yekha) ndi kuyeretsa chipembedzo Chake popendekera ku choona (ndi kusiya njira zonama) ndi kuti asunge swalaat ndiponso apereke chopereka (cha pa chuma) chimenecho ndicho chipembedzo choongoka.

[Ndipo sadalamulidwe mu malamulo enawo kupatula kuti am'pembedze Allah Yekha akulungamika ndi ibaadah yawoyo nkhope Yake, atapendekera ku chikhulupiriro kusiya shirk. Ndikutinso adzipemphera swalaat mwadongosolo, ndi kumapereka Zakaat, ndipo chimenecho ndicho chipembedzo cholungama chomwe chili Chisilamu.]

(6) Ndithu, amene sadakhulupirire (Muhammad SAW) pakati pa anthu a mabuku ndi opembedza mafano (adzalowetsedwa) ku jahena ndi kukhala m'menemo muyaya, iwowo ndiwo zolengedwa zoipa. [Ndithu anthu amene adakanira mwa Ayuda, Akhristu ndi opembedza mafano chilango chawo ndi moto wa jahena akakhalamo m'menemo muyaya. Iwowo ndi zolengedwa zoipitsitsa.]

(7) Ndithu amene akhulupirira (mwa Allah ndi Mtumiki Wake SAW) ndiponso ndi kumachita zabwino, iwo ndiwo zolengedwa zabwino. [Ndithu anthu amene adam'vomereza Allah natsatira Mtumiki Wake (SAW) ndipo nagwira ntchito zolungama, iwowo ndiwo zolengedwa zabwino koposa].

(8) Malipiro awo ali kwa Mbuye wawo (Tsiku Lomaliza pa zimene adatsogoza, monga chikhulupiriro ndi ntchito zabwino), ndi minda ya muyaya momwe ikuyenda pansi pake mitsinje; adzakhala m'menemo muyaya. Allah adzalandira ntchito zawo nawonso adzayamika zabwino Zake ndi kukondweretsedwa nazo (zomwe adzawapatse). Zimenezo ndi za yemwe aope Mbuye wake (Allah).

[Malipiro awo kwa Mbuye wawo Tsiku la Kiyama ndi minda yokhalamo ndi yokhazikika yomwe ili mumapeto okongola. Ikuyenda pansi pa nyumba za chifumu zake mitsinje. Akakhala m'menemo muyaya. Allah adzakondweretsedwa nawo nawalandira ntchito zawo zolungama, nawonso adzakondweretsedwa Naye mu zomwe awalinganizira mu mitundu ya ulemerero. Malipiro abwino amenewo ndi a yemwe waopa Allah nadzitalikitsa zomuchimwira Iye.]

## (99) SUURAT AZZALZALAT

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Likadzagwedezeka dziko lapansi kugwedezeka kwake kwamphamvu.
2 Ndipo nthaka idzatulutsa mitolo yake (zinthu zomwe zidali m'kati mwake, monga akufa ndi miyala ya mtengo wapatali).
3 Ndipo munthu adzanena (mwa mantha ndi kudabwa m'nthawi imeneyo): "Ha! Yatani nthaka (kodi Kiyama yafika)?

1-3 [Pamene nthaka idzatekeseke kutekeseka kwamphamvu, ndikutulutsa zomwe zidali m'kati mwake zakufa komanso miyala ya mtengo wapatali, komanso pamene adzadzifunse munthu mwa mantha kuti : "Kodi ndi chiyani chaichitikira nthakayi"?]

4 Tsiku limenelo idzanena nkhani zake zonse (zabwino kapena zoipa).
5 Pakuti Mbuye wako adzailamula kutero (kuti igwedezeke ndi kunena zimene zinkachitika pamwamba pake).

4-5 [Tsiku la Kiyama idzanena nthaka zomwe zidachitika pamwamba pake zabwino kapena zoipa ndikuti Allah Subhaanahu Wata'aalaa adzailamula kunena zomwe zachitidwa pamwamba pake.]

6 Tsiku limenelo anthu adzachoka (m'manda) ali m'magulu obalalika kuti akasonyezedwe ntchito zawo (ndi kudziwa chiwerengero chawo chimene chili kwa Allah). [Tsiku limenelo adzabwerera anthu kuchokera ku malo wowerengedwera ali mitundu yosiyanasiyana kuti Allah awaonetse zimene adazichita mu zabwino ndi zoipa ndikuti awalipire pa zimenezo.]

7 Choncho, amene akuchita chabwino cholemera ngati kafumbi kakang'ono, adzaona malipiro ake (ndi kuwalandira).
8 Ndipo amene akuchita choipa cholemera ngati kanjere kakang'ono, adzaona malipiro ake (ndi kuwalandira {Allah} sachitira chinyengo aliyense).

7-8 [Amene angagwire ntchito yolemera ngati nyerere yochepa ili yabwino, akaona malipiro ake Tsiku Lomaliza komanso amene angagwire

جَزَآؤُهُمۡ عِندَ رَبِّهِمۡ جَنَّٰتُ عَدۡنٖ تَجۡرِي مِن تَحۡتِهَا ٱلۡأَنۡهَٰرُ خَٰلِدِينَ
فِيهَآ أَبَدٗاۖ رَّضِيَ ٱللَّهُ عَنۡهُمۡ وَرَضُواْ عَنۡهُۚ ذَٰلِكَ لِمَنۡ خَشِيَ رَبَّهُۥ ٨

ترتيبها ٩٩ — سُورَةُ الزَّلۡزَلَةِ — آياتها ٨

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

إِذَا زُلۡزِلَتِ ٱلۡأَرۡضُ زِلۡزَالَهَا ١ وَأَخۡرَجَتِ ٱلۡأَرۡضُ أَثۡقَالَهَا
٢ وَقَالَ ٱلۡإِنسَٰنُ مَا لَهَا ٣ يَوۡمَئِذٖ تُحَدِّثُ أَخۡبَارَهَا ٤
بِأَنَّ رَبَّكَ أَوۡحَىٰ لَهَا ٥ يَوۡمَئِذٖ يَصۡدُرُ ٱلنَّاسُ أَشۡتَاتٗا
لِّيُرَوۡاْ أَعۡمَٰلَهُمۡ ٦ فَمَن يَعۡمَلۡ مِثۡقَالَ ذَرَّةٍ خَيۡرٗا
يَرَهُۥ ٧ وَمَن يَعۡمَلۡ مِثۡقَالَ ذَرَّةٖ شَرّٗا يَرَهُۥ ٨

ترتيبها ١٠٠ — سُورَةُ العَادِيَاتِ — آياتها ١١

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

وَٱلۡعَٰدِيَٰتِ ضَبۡحٗا ١ فَٱلۡمُورِيَٰتِ قَدۡحٗا ٢ فَٱلۡمُغِيرَٰتِ صُبۡحٗا
٣ فَأَثَرۡنَ بِهِۦ نَقۡعٗا ٤ فَوَسَطۡنَ بِهِۦ جَمۡعًا ٥ إِنَّ ٱلۡإِنسَٰنَ
لِرَبِّهِۦ لَكَنُودٞ ٦ وَإِنَّهُۥ عَلَىٰ ذَٰلِكَ لَشَهِيدٞ ٧ وَإِنَّهُۥ لِحُبِّ
ٱلۡخَيۡرِ لَشَدِيدٌ ٨ ۞ أَفَلَا يَعۡلَمُ إِذَا بُعۡثِرَ مَا فِي ٱلۡقُبُورِ ٩

ntchito yolemera ngati nyerere yaing'ono ili yoipa akaona chilango chake Tsiku Lomaliza.

## (100) SUURAT-UL-A'AADIYAAT

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Ndikulumbirira akavalo othamanga uku akutulutsa mpumulo wamphamvu. [Allah walumbirira akavalo othamanga pa njira Yake kunka kumbali ya adani pamene amaonekera poyera mawu ake chifukwa chofulumira kuthamanga kwake. Ndi zosavomerezeka kwa cholengedwa kuti alumbirire pa china chilichonse kupatula pa Allah. Popeza ndithu kulumbirira chinachake chosakhala Allah ndi shirk]
2 Ndikutulutsa moto ku ziboda (pomenyetsa miyendo m'miyala). [Ndiponso akulumbirira akavalo amene umayaka moto kuchokera mu kulimba kwa miyendo yake chifukwa chothamanga kwake kwambiri.]
3 Ndikuwathira nkhondo adani m'mawa (dzuwa lisadatuluke). [Komanso akulumbirira akavalo amene amakaputa adani m'bandakucha].
4 Ndikuwulutsa fumbi lambiri (kwa adani mu nthawi imeneyo) [Akavalowo namatulutsa ndi kuthamanga kumeneku fumbi].

وَحُصِّلَ مَا فِي ٱلصُّدُورِ ﴿١٠﴾ إِنَّ رَبَّهُم بِهِمۡ يَوۡمَئِذٖ لَّخَبِيرُۢ ﴿١١﴾

## سُورَةُ ٱلۡقَارِعَةِ

ترتيبها ١٠١ — آياتها ١١

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

ٱلۡقَارِعَةُ ﴿١﴾ مَا ٱلۡقَارِعَةُ ﴿٢﴾ وَمَآ أَدۡرَىٰكَ مَا ٱلۡقَارِعَةُ
﴿٣﴾ يَوۡمَ يَكُونُ ٱلنَّاسُ كَٱلۡفَرَاشِ ٱلۡمَبۡثُوثِ ﴿٤﴾
وَتَكُونُ ٱلۡجِبَالُ كَٱلۡعِهۡنِ ٱلۡمَنفُوشِ ﴿٥﴾ فَأَمَّا
مَن ثَقُلَتۡ مَوَٰزِينُهُۥ ﴿٦﴾ فَهُوَ فِي عِيشَةٖ رَّاضِيَةٖ
﴿٧﴾ وَأَمَّا مَنۡ خَفَّتۡ مَوَٰزِينُهُۥ ﴿٨﴾ فَأُمُّهُۥ هَاوِيَةٞ
﴿٩﴾ وَمَآ أَدۡرَىٰكَ مَا هِيَهۡ ﴿١٠﴾ نَارٌ حَامِيَةُۢ ﴿١١﴾

## سُورَةُ ٱلتَّكَاثُرِ

ترتيبها ١٠٢ — آياتها ٨

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

أَلۡهَىٰكُمُ ٱلتَّكَاثُرُ ﴿١﴾ حَتَّىٰ زُرۡتُمُ ٱلۡمَقَابِرَ ﴿٢﴾ كَلَّا سَوۡفَ
تَعۡلَمُونَ ﴿٣﴾ ثُمَّ كَلَّا سَوۡفَ تَعۡلَمُونَ ﴿٤﴾ كَلَّا لَوۡ تَعۡلَمُونَ
عِلۡمَ ٱلۡيَقِينِ ﴿٥﴾ لَتَرَوُنَّ ٱلۡجَحِيمَ ﴿٦﴾ ثُمَّ لَتَرَوُنَّهَا
عَيۡنَ ٱلۡيَقِينِ ﴿٧﴾ ثُمَّ لَتُسۡـَٔلُنَّ يَوۡمَئِذٍ عَنِ ٱلنَّعِيمِ ﴿٨﴾

(5) Ndikulowerera m'katikati mwa adani. [Ndikuwaika pakati limodzi ndi amene awakwera magulu a adani].

(6) Ndithu munthu ali wokanira mtendere wa Mbuye wake (sathokoza Allah pa zimene amudalitsa nazo).

(7) Ndithudi iye pa zimenezo ndi mboni (yodzichitira yekha kupyolera m'zochitachita zake).

(8) Ndipo ali wokonda chuma kwambiri (ndiponso ngwamsulizo).

6-8 [Ndithu munthu pa mitendere ya Mbuye wake ndi wokanira kwambiri, ndiponso ndithu iyeyu za kukanira kwakeku ndi wovomereza. Ndipo ndithu iye pokonda chuma ndi wochilimika].

(9) Kodi sakudziwa zikadzatulutsidwa za m'manda. [Kodi sakudziwa munthu zomwe zikumuyembekezera pamene Allah adzatulutse akufa kuchokera ku manda kuti akawerengeredwe ndi kulipidwa.]

(10) Ndi kudzasonkhanitsidwa ndi kudzaonekera poyera zomwe zidali m'mitima? [Ndi kudzatulutsidwa zimene zidabisika m'mitima mu zabwino kapena zoipa.]

(11) Tsiku limenelo Mbuye wawo adzawadziwa kwambiri (ndikuwalongosolera zonse zochita zawo). [Ndithu Mbuye wawo za iwo ndi ntchito zawo tsiku limenelo ndi Wozidziwa kwambiri palibe mwa zimenezo kanthu kakabisike kwa Iye.]

## (101) SUURAT-UL-QAARIA'H

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Kugunda kwa phokoso (la Kiyama).
[Nthawi imene Kiyama idzagunde mitima ya anthu ndi zoopsa zake]

(2) Kodi kugunda kwa phokosolo (la Kiyama) n'chiyani (kuopsa kwake).
[Ndi chinthu chanji kugunda kumeneku?]

(3) N'chiyani chingakudziwitse za kugunda kwa phokoso (la Kiyama komwe kudzawakomole anthu)?
[Ndipo ndi chinthu chanji chakudziwitsa nacho?]

(4) Limenelo ndi tsiku limene anthu adzakhala ngati agulugufe obalalika (ena kunka chakumanja ena ku manzere, ena patsogolo ena m'mbuyo).
[Mu tsiku limenelo, anthu adzakhala mu unyinji wawo ndi kutayana kwawo komanso kutekeseka kwawo ngati agulugufe ofalikira ponseponse, ameneyo ndi amene akagwere m'moto.]

(5) Ndipo mapiri adzakhala ngati ubweya opakidwa utoto, omwazidwa (ongouluzika uku ndi uku mu mlengalenga). [Ndipo mapiri adzakhala ngati ubweya wa mitundu yosiyanasiyana umene umazulidwa ndi dzanja nkukhala fumbi lokhalokha ndi kuchoka].

(6) Tsono amene muyeso wake (wa zinthu zabwino) udzalemere (ndi kupepuka zoipa)

(7) (Ndiye kuti) adzakhala mu umoyo wosangalatsa (pa tsiku la chiweruzo).

6-7 [Tsono munthu amene idzalemere sikelo ya zabwino zake, ndiye kuti iyeyo akakhala mu umoyo wosangalatsa mu jannah.]

(8) Ndipo yemwe muyeso wake (wa zinthu zabwino) udzapepuke ndi kulemera zoipa,

(9) Ndiye kuti mbuto yake ndi ku haawiya.

8-9 [Tsono munthu amene idzapepuke sikelo ya zabwino zake ndi kulemera sikelo ya zoipa zake, ndiye malo ake ndi ku jahena].

(10) Kodi ndi chiyani chakudziwitsa za haawiya?
[Ndi chiyani chitakudziwitse iwe Mtumiki (SAW) kuti haawiya imeneyi ndi chiyani?]

1 Umenewo ndi moto woyaka mwaukali.
[Ndithudi umenewu ndi moto wayaka kwambiri kuchokera ku nkhuni zomwe zili pa umenewo].

## (102) SUURAT – TAKAATHUR

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

(1) Kwakutangwanitsani kusonkhanitsa chuma chambiri ndi ana. [Chakutangwanitsani kusiya kumvera Allah kunyaditsana ndi kuchuluka kwa chuma ndi ana]

2 Mpakana mwapita ku manda (mpakana mwamwalira ndikukalowa m'manda).
[Kutangwanika kwanu kwapitirira ndi zimenezo kufikira mutakakhala ku manda ndi kuikidwa m'menemo].
3 Sichoncho! Mudziwa posachedwapa.
[Simoteremu kudayenera kuti chisakutangwanitseni chuma, posachedwa mudzazindikira kuti nyumba ya Tsiku Lomaliza ndi yabwino kwa inu koposa.]
4 Ndiponso sichoncho! Mudziwa posachedwapa.
[Kenaka, pewan,i posachedwa mudziwa mapeto woipa a kutanganidwa kwanuku.]
5 Sichoncho! Mukadadakhala mukudziwa, kudziwa kwa chitsimikizo (sibwenzi mukutangwanika ndi za m'dziko).
6 Ndithudi mudzaona moto,
7 Kenako mudzaona ndithu ndi diso la chitsimikizo.
8 Tsono pa tsikulo ndithudi mudzafunsidwa za chisomo (mtendere) chomwe munapatsidwa nacho kuti mudachigwiritsa ntchito motani.)
5-8 [Simoteremu kudayenera kuti kusakutangwanitseni kuchulukitsa chuma mukadadakhala mukudziwa, kudziwa kwa choonadi bwenzi mutabwerera m'mbuyo ndipo mukadafulumizitsira kuzidzidzimutsa eni akenu ku chiongoko. Mtheradi mudzaiona jahena kenako mudzaionadi mopanda chikaiko. Kenako mudzafunsidwa Tsiku la Kiyama za mitundu yonse ya chisomo].

## (103) SUURAT-UL-ASR

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**
1 Ndikuilumbirira nthawi.
2 Ndithu, munthu aliyense ndi wotaika (chifukwa cha kugonjetsedwa ndi zilakolako zake).
1-2 [Allah wailumbirira nyengo kuti ndithu ana a Adam (AS) ali mu chionongeko ndi kupunguka. Ndipo ndizosavomerezeka kwa kapolo kuti alumbirire pa china chilichonse kupatula Allah. Popeza ndithu kulumbirira china chake chosakhala Allah ndi shirk.
3 Kupatula amene akhulupirira mwa Allah ndi kumachita zabwino, ndi kumalangizana kutsatira choona ndiponso ndi kumalangizana za kupirira (potsatira malamulo a Allah ndi zina zovuta za m'dziko).
[Kupatula anthu amene adamukhulupirira Allah ndi kugwira ntchito zolungama komanso akulangizana wina ndi mnzake zogwiritsa choonadi ndi kugwiritsa ntchito za kumvera Allah ndi kupirira pa zimenezo].

سُورَةُ العَصۡرِ — ترتيبها ١٠٣ — آياتها ٣

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

وَٱلۡعَصۡرِ ﴿١﴾ إِنَّ ٱلۡإِنسَٰنَ لَفِي خُسۡرٍ ﴿٢﴾ إِلَّا ٱلَّذِينَ ءَامَنُواْ
وَعَمِلُواْ ٱلصَّٰلِحَٰتِ وَتَوَاصَوۡاْ بِٱلۡحَقِّ وَتَوَاصَوۡاْ بِٱلصَّبۡرِ ﴿٣﴾

سُورَةُ الهُمَزَةِ — ترتيبها ١٠٤ — آياتها ٩

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

وَيۡلٞ لِّكُلِّ هُمَزَةٖ لُّمَزَةٍ ﴿١﴾ ٱلَّذِي جَمَعَ مَالٗا وَعَدَّدَهُۥ ﴿٢﴾
يَحۡسَبُ أَنَّ مَالَهُۥٓ أَخۡلَدَهُۥ ﴿٣﴾ كَلَّاۖ لَيُنۢبَذَنَّ فِي ٱلۡحُطَمَةِ ﴿٤﴾
وَمَآ أَدۡرَىٰكَ مَا ٱلۡحُطَمَةُ ﴿٥﴾ نَارُ ٱللَّهِ ٱلۡمُوقَدَةُ ﴿٦﴾ ٱلَّتِي تَطَّلِعُ
عَلَى ٱلۡأَفۡـِٔدَةِ ﴿٧﴾ إِنَّهَا عَلَيۡهِم مُّؤۡصَدَةٞ ﴿٨﴾ فِي عَمَدٖ مُّمَدَّدَةِۭ ﴿٩﴾

سُورَةُ الفِيلِ — ترتيبها ١٠٥ — آياتها ٥

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

أَلَمۡ تَرَ كَيۡفَ فَعَلَ رَبُّكَ بِأَصۡحَٰبِ ٱلۡفِيلِ ﴿١﴾ أَلَمۡ يَجۡعَلۡ كَيۡدَهُمۡ
فِي تَضۡلِيلٖ ﴿٢﴾ وَأَرۡسَلَ عَلَيۡهِمۡ طَيۡرًا أَبَابِيلَ ﴿٣﴾ تَرۡمِيهِم
بِحِجَارَةٖ مِّن سِجِّيلٖ ﴿٤﴾ فَجَعَلَهُمۡ كَعَصۡفٖ مَّأۡكُولِۭ ﴿٥﴾

## (104) SUURAT –UL HUMAZAH

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**
1 Kuonongeka koopsa kudzam'peza wina aliyense wojenda anthu ndi wonyoza anthu polozera (ndi maso kapena kuyankhula ndi lirime).
[Zoipa ndi kuonongeka kuli kwa wina aliyense wojeda anthu, wowanyogodola].
2 Yemwe wasonkhanitsa chuma ndi kumachiwerengera (pokhumbiza anthu ena popanda kuchigwiritsa ntchito m'njira zabwino)
[Amene kuli kujjirika ndi cholinga chake kusonkhanitsa chuma ndi kumachiwerengera]
3 Akuganiza kuti chuma chakecho chimukhazikitsa (pa dziko) muyaya (ndi kumuteteza ku zimene sakuzifuna).
[Akuganiza kuti wadziikira yekha chikhulupiriro ndi chuma chimene wachisonkhanitsachi kuti chimukhazikitsa muyaya pa dziko lapansi ndikuti adzazemba wosawerengedwa].
4 Sichoncho! (asiye maganizo amenewo) ndikulumbirira ndithu, akaponyedwa ku moto woononga (chifukwa cha kuipa kwa zochita zake). [Zinthu sizili monga m'mene

akuganizira mtheradi adzaponyedwa m'moto womwe ukanyenyenyenye chilichonse choponyedwa m'menemo].

5 Ndi chiyani chingakudziwitse za moto woonongawu? [Ndi chiyani chingakudziwitse iwe Mtumiki (SAW) kuti chenicheni cha motowo n'chiyani?]

6 Umenewo ndi moto wa Allah woyaka (nthawi zonse, woononga chilichonse choponyedwa m'menemo).

7 Umene umakwera mpaka ku mtima.

6-7 [Ndithu umenewo ndi moto wa Allah woyaka womwe chifukwa cha ukali wake uzikapita kuchokera ku matupi mpaka ku mitima.]

8 Ndithu, motowo ukawazinga (ndi kuwatsekera makomo).

9 Ndipo (akamangidwa) m'nsanamira zitalizitali (kotero kuti sakatha kugwedezeka m'menemo kapena kupulumuka).

8-9 [Ndithu motowo ukakhala wotsekedwa bwino mu maunyolo komanso magoli otalikitsidwa kuti asathe kutuluka m'menemo].

## (105) SUURAT-UL-FIIL

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Kodi siudaone momwe Mbuye wako adawachitira eni njovu? [Kodi siudadziwe iwe Mtumiki (SAW) m'mene adachitira Mbuye wako ndi eni njovu –Abrahah Al-Habashiy ndi gulu lake la nkhondo amene adafuna kugumula Kaaba Yolemekezeka?

2 Kodi sadachichite chiwembu chawo kukhala chopanda phindu (chosokera)? [Kodi sadazichite zimene adazikonzazo mu zoipa kukhala zopanda phindu komanso zopanda pake?]

3 Adawatumizira magulumagulu a mbalame otsatizana (ndipo adawazungulira mbali zonse).

4 Zidawagenda ndi miyala ya moto.

3-4 [Ndipo adawatumizira iwowo mbalame mu magulumagulu mondondozana, zikuwaponya iwowo ndi miyala ya dongo yowotchedwa nkusanduka miyala yolimba.]

5 Adawachita ngati m'mera wodyedwa (ndi nyama ndi kulavulidwa).

[Ndipo adawachita ndi miyalayo kukhala oteketulidwa ngati masamba a m'mera ouma omwe ziweto zawadya nkulavula].

## (106) SUURAT-UL-QURAISH

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Cholinga chakuwachita ma Quraish kuti apitirize chizolowezi chawo.

2 Chizolowezi chawo choyenda nthawi ya dzinja (kunka ku Yemen) ndi chizolowezi chawo choyenda nthawi ya chirimwe (kunka ku Shaam kukachita malonda, mosatekeseka ndi mopanda mantha).

1-2 [Kondweretsedwani ndi cholinga chakuwachita ma Quraish kuti apitirize chizolowezi chawo komanso chitetezo chawo ndi kukhazikika kwa zinthu zokomera iwo. Komanso kukhazikika kwa dongosolo la ulendo wawo mu nthawi ya dzinja kunka ku Yemen komanso nthawi ya chirimwe kunka ku Shaam, ndi kuwafewetsera zimenezo kuti akatenge zomwe akuzisowa].

3 Choncho, amupembedze Mbuye wa nyumba iyi (Al-Kaaba Amene adachititsa kuti athe kuyenda maulendo awiriwo).

Choncho ayenera kuthokoza komanso am'pembedze Mbuye wa nyumba iyi yomwe ndi Kaaba imene iwowo alemekezeka nayo. Ndinso am'chite kukhala wayekha ndi kumuyeretsera Iye ibaadah.

4 Yemwe amawadyetsa (nthawi imene Arab anzawo) ali mu njala, amawapatsa chitetezo (pomwe anzawo) ali ndi mantha.

[Yemwe amawadyetsa ku njala yoopsa komanso kuwapatsa chitetezo ku kukutekeseka ndi mantha akulu.]

## (107) SUURAT-UL-MAAU'UN

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Kodi wamuona yemwe akutsutsa za mphoto (ndi chiwerengero cha Tsiku Lomaliza)?

[Kodi wamuona kakhalidwe ka uyo amene akukanira za kuuka kwa akufa ndi malipiro?]

2 Iye ndi yemwe akukankha wamasiye (mwa nkhanza).[Ameneyo ndi amene akukankha wamasiye mwa mphamvu komanso mwa nkhanza kumutsekereza kupeza gawo lake chifukwa cha kuuma mtima wake.]

3 Salimbikitsa (ena pamodzi ndi iye mwini) kudyetsa wosauka. [Ndipo iye salimbikitsa anzake zodyetsa wosauka, ndiye zingatheke bwanji kuti iyeyo amudyetse iye mwini?]

4 Choncho kuonongeka kuli pa ena mwa opembedza (amene ali ndi mbiri izi):

5 Omwe amachitira mphwayi mapemphero awo (popemphera modukizadukiza ndipo sapeza phindu ndi mapemphero awowo).

[Ndipo chilango choopsa chili kwa opemphera amene za swalaat yawo amachitira chibwana, saswali swalaat zimenezi moyenerera mwake ndipo saziswali swalaatizi mu nthawi zake].

6 Amenenso (akachita mapemphero awo) amadzionetsera (kwa anthu mwa chiphamaso kuti apeze ulemerero ndi kutamandidwa m'mitima mwa anthu).[Anthu amene akudzionetsera ndi ntchito zabwino kuti anthu awatame].

7 Amamana ziwiya (zawo posawabwereka anzawo zinthu zofunika pa moyo wa aliyense monga nkhwangwa, mpeni, mtondo ndi zina zotero).[Ndipo amakaniza kubwereketsa zomwe sizingavutitse kuzibwereketsa mu ziwiya ndi zina zotero. Tero iwo sadalongosole ibaadah yopangira Mbuye wawo komanso sadathe kuchitira zabwino zolengedwa Zake.]

## (108) SUURT-UL KAUTHAR

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Ndithu, takupatsa zabwino zambiri zina mwa izo ndi mtsinje wotchedwa Kauthar. [Ndithu Ife takupatsa iwe Mtumiki (SAW) zabwino zambiri pa dziko lapansi komanso Tsiku Lomaliza zina mwa izo ndi mtsinje wa Kauthar mu jannah womwe mbali zake ziwiri muli matenti a ngale zopanda kanthu m'kati mwake komanso dothi lake ndi misk]

2 (Pakuti ndakupatsa zimenezo) pitiriza kupembedza Mbuye wako (moyera mtima) ipha nsembe yako (chifukwa chakuthokoza Allah pazimene wakupatsa monga ulemerero ndi kukusankhira zabwino zambiri)
[Choncho umuyeretsere Mbuye wako swalaat zako zonse, ndiponso zinga nyama yako chifukwa cha Iye komanso pa dzina Lake lokha.]

3 Ndithu, iye amene akukuda iwe ndiye ali wopanda mwayi.[Ndithu woda iwe ndi wodana nazo zimene wazibweretsa mu za chiongoko ndi dangalira, iye ndi amene ali woduka mapazi ake, wodulidwa ku zabwino zonse]

## (109) SUURAT-UL KAAFIRUUN

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Nena (iwe Muhammad SAW): E!, Inu anthu osakhulupirira (amene mukupitiriza kukanira kwanu) [Nena iwe Mtumiki (SAW) kwa anthu amene adakanira Allah ndi Mtumiki Wake (SAW): "E, inu okanira Allah!"]

2 sindipembedza chimene inu mukuchipembedza (posiya Allah). [Ine sindipembedza zimene inu mukuzipembedza mu mafano komanso milungu yopeka].

3 Inunso simupembedza Amene ine ndikumupembedza (Yemwe ndi Allah m'modzi.) [Ngakhalenso sikuti mukupembedza wopembedzedwa m'modzi Amene ali Allah Mbuye wa zolengedwa zonse woyenerera Iye Yekhayo kupembedzedwa].

4 Ndiponso ine sindidzapembedza chimene inu mwakhala mukuchipembedza (chifukwa inu ndinu ophatikiza Allah ndi zinthu zina).

سُورَةُ قُرَيۡشٍ — ترتيبها ١٠٦ — آياتها ٤

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

لِإِيلَٰفِ قُرَيۡشٍ ١ إِۦلَٰفِهِمۡ رِحۡلَةَ ٱلشِّتَآءِ وَٱلصَّيۡفِ
٢ فَلۡيَعۡبُدُواْ رَبَّ هَٰذَا ٱلۡبَيۡتِ ٣ ٱلَّذِيٓ أَطۡعَمَهُم
مِّن جُوعٖ وَءَامَنَهُم مِّنۡ خَوۡفِۭ ٤

سُورَةُ المَاعُونِ — ترتيبها ١٠٧ — آياتها ٧

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

أَرَءَيۡتَ ٱلَّذِي يُكَذِّبُ بِٱلدِّينِ ١ فَذَٰلِكَ ٱلَّذِي
يَدُعُّ ٱلۡيَتِيمَ ٢ وَلَا يَحُضُّ عَلَىٰ طَعَامِ ٱلۡمِسۡكِينِ ٣
فَوَيۡلٞ لِّلۡمُصَلِّينَ ٤ ٱلَّذِينَ هُمۡ عَن صَلَاتِهِمۡ سَاهُونَ
٥ ٱلَّذِينَ هُمۡ يُرَآءُونَ ٦ وَيَمۡنَعُونَ ٱلۡمَاعُونَ ٧

سُورَةُ الكَوۡثَرِ — ترتيبها ١٠٨ — آياتها ٣

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

إِنَّآ أَعۡطَيۡنَٰكَ ٱلۡكَوۡثَرَ ١ فَصَلِّ لِرَبِّكَ وَٱنۡحَرۡ ٢
إِنَّ شَانِئَكَ هُوَ ٱلۡأَبۡتَرُ ٣

[Ngakhalenso ine sikuti ndingapembedze zimene inu mukuzipembedza mu mafano komanso milungu yabodza].

5 Ndipo inu simudzamupembedza Amene ine ndikumupembedza (chifukwa ndi chipembedzo chopembedza Allah m'modzi). [Ngakhalenso inu sikuti mudzapembedza mtsogolo chomwe ine ndikuchipembedza. Ndipo Ayah imeneyi idavumbulutsidwa mwa anthu okhudzidwa ndi maina awo mwa anthu opembedza mafano, ndithudi Allah adadziwa kuti iwowo sadzakhulupirira mpaka kalekale].

6 Inu muli ndi chipembedzo chanu (chimene mukuchikhulupirira) inenso ndili ndi chipembedzo changa (chimene Allah wandisankhira). [Inutu muli ndi chipembedzo chanu chimene mwakakamira kuchitsatira ndiponso ine ndili ndi chipembedzo changa chimene sindingafune china m'malo mwa icho].

## (110) SUURAT – ANNASAR

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Chikadza chipulumutso cha Allah ndi kugonjetsa (mzinda wa Makka kwa iwe ndi

سُورَةُ الكَافِرُونَ — ترتيبها ١٠٩ — آياتها ٦

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

قُلۡ يَٰٓأَيُّهَا ٱلۡكَٰفِرُونَ ١ لَآ أَعۡبُدُ مَا تَعۡبُدُونَ ٢
وَلَآ أَنتُمۡ عَٰبِدُونَ مَآ أَعۡبُدُ ٣ وَلَآ أَنَا۠ عَابِدٞ مَّا عَبَدتُّمۡ ٤
وَلَآ أَنتُمۡ عَٰبِدُونَ مَآ أَعۡبُدُ ٥ لَكُمۡ دِينُكُمۡ وَلِيَ دِينِ ٦

سُورَةُ النَّصۡرِ — ترتيبها ١١٠ — آياتها ٣

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

إِذَا جَآءَ نَصۡرُ ٱللَّهِ وَٱلۡفَتۡحُ ١ وَرَأَيۡتَ ٱلنَّاسَ
يَدۡخُلُونَ فِي دِينِ ٱللَّهِ أَفۡوَاجٗا ٢ فَسَبِّحۡ بِحَمۡدِ رَبِّكَ
وَٱسۡتَغۡفِرۡهُۚ إِنَّهُۥ كَانَ تَوَّابَۢا ٣

سُورَةُ المَسَدِ — ترتيبها ١١١ — آياتها ٥

بِسۡمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحۡمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

تَبَّتۡ يَدَآ أَبِي لَهَبٖ وَتَبَّ ١ مَآ أَغۡنَىٰ عَنۡهُ مَالُهُۥ وَمَا
كَسَبَ ٢ سَيَصۡلَىٰ نَارٗا ذَاتَ لَهَبٖ ٣ وَٱمۡرَأَتُهُۥ
حَمَّالَةَ ٱلۡحَطَبِ ٤ فِي جِيدِهَا حَبۡلٞ مِّن مَّسَدِۭ ٥

okutsatira). [Chikadzakwanira kwa iwe Mtumiki (SAW) chipulumutso pa makafiri a chi Quraish, ndipo ndikukwanirira kwa iwe kugonjetsa mzinda wa Makka.]

2 Ndipo ukawaona anthu akulowa chipembedzo cha Allah ali m'magulumagulu.

[Ndipo ukadzaona anthu ambiri akulowa mu Chisilamu makhamumakhamu].

3 (Pamenepo) lemekeza Mbuye wako ndi kum'tamanda ndiponso m'pemphe chikhululuko, ndipo Iye ndi Wolandira mochuluka kulapa (kwa anthu Ake).

[Zikadzachitika zimenezo, ndiye kuti ukonzeke zokumana ndi Mbuye wako pochulukitsa kuchita tasbeeh (kumuyeretsa Allah) ndikumutamanda ndi kuchulukitsa kumupempha chikhululuko. Ndithu Iyeyo ndi Wolandira kulapa kwa anthu omuyeretsa ndi omupempha chikhululuko, amawalandira kulapa kwawo iwowo ndi kuwachitira chifundo ndi kuwalandira kubwerera kwawo kwa Iye.]

## (111) SUURAT-UL-MASAD

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Aononongeka manja a Abii Lahabi (omwe adali kuwagwiritsa ntchito pozunza Asilamu) nayenso waonongeka.

[Ataika manja a Abii Lahabi ndiponso waipa chifukwa chozunza kwake Mtumiki wa Allah Muhammad (SAW). Ndithudi kunatsimikizika kutaika kwa Abii Lahabi.

2 Chuma chake ndi ulemerero wake (umene adaupeza) sizidam'tchinjirize ku chilango cha Allah.

[Sichidamuthandize chuma chake ndi ana ake ndipo ziwirizi sizidzamutchinjiriza iyeyo kanthu kalikonse mu chilango cha Allah chikadzamufikira].

3 (Akadzamwalira) adzalowa ku moto woyaka kwambiri (ndipo adzaotchedwa ndi motowo).

4 Nayenso mkazi wake (adzalowa ku moto) yemwe adali kusenza nkhuni (zaminga pomutchera Mtumiki (SAW) komanso amanka nadanitsa pakati pa anthu).

3-4 [Adzalowa ku moto woyaka kwambiri iyeyo ndi mkazi wake yemwe adali kunyamula minga ndi kumaiponya mu njira ya Mtumiki (SAW) chifukwa chofuna kumuzunza.

5 M'khosi mwake mudzamangidwa chingwe chopiringidwa bwino cha mulaza (chom'langa nacho).

[M'khosi mwake mudzakhala chingwe chopotedwa bwino ndi mulaza wokhuthara akanyamulidwa nawo mu moto wa jahena kenako nakaponyedwa pansi pake pa jahenayo].

## (112) SUURAT-UL- IKHLAAS

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**

1 Nena (Iwe Muhammad SAW kwa amene akukufunsa mwachipongwe, mbiri za Allah wako) Iye ndi Allah m'modzi (alibe mnzake).

[Nena iwe Mtumiki (SAW) Ameneyotu ndi Allah Wayekhayekha ndi kupembedzedwa komanso usungi Wake ndinso mu maina ndi mbiri, palibe amene amasakanikirana naye mu zimenezo.]

2 Allah ndi Wokhala ndi zonse, Wodalirika ndi zolengedwa Zake.

[Allah Yekhayo ndi amene amayang'anidwa maso pochita china chilichonse chothandiza zolengedwa zonse ndi zokhumba zawo.]

3 Sadabale (mwana) ndiponso sadaberekedwe (ndi mayi).

[Alibe mwana ngakhalenso m'bereki komanso alibe mkazi].
4 Ndiponso palibe aliyense wofanana ndi Iye.
[Ndiponso Iye alibe wofanana Naye kapena kutengerana m'maonekedwe ndi wina aliyense mwa zolengedwa Zake osati mu maina Ake ngakhalenso mu mbiri Zake nanjinso mu zochita Zake. Iye ndi Wolemekezeka,Wotukuka komanso Woyeretsedwa].

## (113) SUURAT-UL-FALAQ

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**
1 Nena : "Ndikudzitchinjiriza ndi Mbuye wa m'bandakucha. [Nena iwe Mtumiki (SAW) kuti: "Ndikudzitchinjiriza ndi kugwiritsa ndi Bwana wa m'bandakucha umene uli kuyera kwa kucha].
2 "Kuchokera ku zoipa zimene Iye adazilenga
[Ku zoipa za zolengedwa zonse ndi masautso ake].
3 "Ndi ku zoipa za usiku pamene mdima ukulowa mwamphamvu.
[ Ndi ku zoipa za usiku wa mdima wambiri ukalowa ndi kukhazikika ndi zomwe zili m'menemo mu zoipa ndi zosautsa].
4 "Ndi ku zoipa za afiti omwe amauzira mu fundo. [Ndi zosautsa za afiti achikazi amene amauzira mu zinthu zomwe amazimanga mu fundo ndi cholinga cholodza]
5 " Ndiponso ku zoipa za wa nsanje pamene akuchita nsanje (ndi kufuna kuti ena mtendere uwachoke umene Allah wawapatsa)."
[Ndi ku zoipa za munthu wa kaduka, woda anthu pamene akuwachitira kaduka pa zomwe Allah wawaninkha mu mitendere ndipo iye akufuna kuti ichoke kwa iwo ndi kuwagwetsera mazunzo pa iwo.]

## (114) SUURAT –ANNAAS

**M'dzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni.**
1 Nena: "Ndikudzitchinjiriza ndi Mbuye (Mleri) wa anthu (Yemwe akulinganiza zinthu zawo).
[Nena iwe Mtumiki (SAW) kuti: "Ndikudzitchinjiriza komanso kugwiritsa ndi Bwana wa anthu, Amene ali ndi kuthekera Yekhayo pobweza zoipa za manong'onong'o].
2 "Mfumu ya anthu onse. [Mfumu ya anthu onse Yemwe amawachitira zonse zokhudza iwowo koma Iyeyu ndi Wosadalira iwo.]
3 "Wopembedzedwa wa anthu (Amene ali ndi mphamvu zochitira chilichonse pa iwo).
[Wopembedzedwa wa anthu Amene palibe wina wopembedzedwa mwa choonadi kupatula Iye].
4 "Ku zoipa za m'nong'onezi (yemwe amathira unong'onezi wake m'mitima ya anthu yemwenso amabisala posiya unong'onezi wake ngati mwini mtimawo atam'kumbukira Allah).
[Ku zoipa za satana amene amanong'oneza pa nthawi ya kusalabadira ndipo amabisala pa nthawi yomutchula Allah].
5 "Yemwe amanong'oneza mu zifuwa za anthu.
[Yemwe amautsa zoipa ndi zikaiko m'mitima ya anthu].
6 "Wochokera mu ziwanda ndi mwa anthu".
[Mu magulu asatana a ziwanda komanso anthu].
Womasulira Ndemanga za Qur'aan ma Juzu atatu amenewa m'Chichewa ndi Sheikh Hanif Kazembe.

### سُورَةُ الإخلاص

ترتيبها ١١٢ — آياتها ٤

بِسْمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحْمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

قُلْ هُوَ ٱللَّهُ أَحَدٌ ﴿١﴾ ٱللَّهُ ٱلصَّمَدُ ﴿٢﴾ لَمْ يَلِدْ وَلَمْ يُولَدْ ﴿٣﴾ وَلَمْ يَكُن لَّهُۥ كُفُوًا أَحَدٌۢ ﴿٤﴾

### سُورَةُ الفَلَق

ترتيبها ١١٣ — آياتها ٥

بِسْمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحْمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

قُلْ أَعُوذُ بِرَبِّ ٱلْفَلَقِ ﴿١﴾ مِن شَرِّ مَا خَلَقَ ﴿٢﴾ وَمِن شَرِّ غَاسِقٍ إِذَا وَقَبَ ﴿٣﴾ وَمِن شَرِّ ٱلنَّفَّٰثَٰتِ فِى ٱلْعُقَدِ ﴿٤﴾ وَمِن شَرِّ حَاسِدٍ إِذَا حَسَدَ ﴿٥﴾

### سُورَةُ النَّاس

ترتيبها ١١٤ — آياتها ٦

بِسْمِ ٱللَّهِ ٱلرَّحْمَٰنِ ٱلرَّحِيمِ

قُلْ أَعُوذُ بِرَبِّ ٱلنَّاسِ ﴿١﴾ مَلِكِ ٱلنَّاسِ ﴿٢﴾ إِلَٰهِ ٱلنَّاسِ ﴿٣﴾ مِن شَرِّ ٱلْوَسْوَاسِ ٱلْخَنَّاسِ ﴿٤﴾ ٱلَّذِى يُوَسْوِسُ فِى صُدُورِ ٱلنَّاسِ ﴿٥﴾ مِنَ ٱلْجِنَّةِ وَٱلنَّاسِ ﴿٦﴾

# MAFUNSO OFUNIKA MU UMOYO WA MSILAMU

1 **Kodi Msilamu chikhulupiriro chake amachitenga kuti?** Msilamu amatenga chikhulupiriro chake kuchokera mu Quràn ndi Hadith yangwiro ya Mneneri wake (SAW) amene sayankhula za kufuna kwake monga ikunenera Ayat kuti: "*Quràn'yo sichina koma chivumbulutso chimene chikuvumbulutsidwa*." **(Surat 53 :4)**.

Ndipo zimenezo zikugwirizana ndi kumva kwa Maswahaaba ndi anthu abwino amene anadza pambuyo pa Maswahaaba (RA).

2 **Kodi tikasiyana maganizo tingabwerere ku chinthu chanji kuti tipeze yankho?** Tibwerere ku Deen yoyera. Chigamulo pa zimenezo tichipereke ku Buku la Allah ndi Sunnat ya Mtumiki Wake (SAW), pakuti Allah wanena kuti, "*Ngati mutatsutsana pa chinthu chili chonse, chibwezereni kwa Allah ndi Mtumiki (Wake)*" **(Surat 4:59)**.

Nayenso Mtumiki (SAW) anati: "*Ndakusiyirani pakati panu zinthu ziwiri simudzasokera ngati mukuzigwiritsira ntchito, Buku la Allah ndi Sunnat ya Mneneri Wake*. "**(Muwattai)**

3 **Kodi ndi gulu liti lomwe lidzapulumuke pa tsiku la Kiyaamat?** Mtumiki (SAW) anati, "*Ummat wanga udzagawikana magulu makumi asanu ndi awiri kudza mphambu zitatu (73), onsewo akalowa ku moto kupatula gulu limodzi*. Maswahaaba anati: "Kodi ndi gulu liti limenelo, Inu Mtumiki wa Allah?" Mtumiki (SAW) anati; "*Lomwe lidzachite zomwe ine ndikuchita ndi Maswahaaba anga*" **(Ahmad, Tirmidhi).** Choncho zoona ndi zomwe anali kuchita Mtumiki (SAW) ndi Maswahaaba ake kotero iwe m'bale wanga uyenera kutsatira zimenezo, ndipo upewe za Bidah ngati ukufuna chipulumutso ndi kulandiridwa ntchito zako.

4 **Kodi n'zofunikira zanji kuti ntchito yabwino ilandiridwe ndi Allah?** Zofunikira zake ndi izi: **1.** Kukhulupirira mwa Allah ndikumuchita kukhala wa yekha, choncho ntchito ili yonse yabwino singalandiridwe kuchokera kwa mushrik (munthu wopembedza mafano). **2.** Kuchita Ikhlaas: ndiko kuti afune ndi ntchito yabwinoyo nkhope ya Allah. **3.** Kutsatira Mneneri (SAW) pogwira ntchitoyo; uku ndiko kuti ikhale yogwirizana ndi zomwe anabweretsa, kotero kuti Allah asapembedzedwe m'njira zina kupatula zimene anakhazikitsa. Ngati chimodzi mwa zimenezi chitasowa ndiye kuti ntchito imeneyo ndiyobwezedwa siingalandiridwe. Allah akunena kuti: "*Ndipo tidzaidzera ntchito iliyonse ya bwino imene anachita, ndipo tidzaichita monga fumbi louluka*." **(Surat 25:23).**

5 **Kodi Deen ya Chisilamu ili ndi magawo angati?** Deen ya Chisilamu ili ndi magawo atatu: Chisilamu, Imaan, ndi Ihsaan.

6 **Kodi Chisilamu ndichiyani? Nanga nsichi zake zilipo zingati?** Chisilamu ndiko kudzipereka kwa Allah movomera umodzi Wake, kugonjera kwa Iye pomumvera ndi kudzitalikitsa ku Shirk ndi eni Shirk.

Nsichi zake zilipo zisanu, Mneneri (SAW) anazitchula m'mau ake onena kuti: "*Chisilamu chamangika pamwamba pa zinthu zisanu izi: 'Kuikira umboni kuti palibe woyenera kupembedzedwa mwa choonadi koma Allah ndi kuti Muhammad ndi Mtumiki Wake, Kuswali kasanu patsiku. Kupereka Zakaat. Kukachita Hajj ndi kusala m'mwezi wa Ramadhan*." **((Bukhaari) ndi Muslim).**

7 **Kodi Imaan ndi chiyani? Nanga nsichi zake zilipo zingati?** Imaan ndiko kukhulupirira kwa mtima, kuyankhula kwa lirime ndi ntchito ya ziwalo. Imaan'yo

imaonjezereka chifukwa cha kumvera malamulo a Allah, ndipo imapunguka chifukwa chonyozera malamulo a Allah. Allah akunena kuti: *"....... adzaonjezera Imaan pamwamba pa Imaan yawo."* (Surat 48 - 4). Ndipo Mtumiki (SAW) anati, "*Imaan ili ndi nthambi zopitirira makumi asanu ndi awiri, nthambi yomwe ili pamwamba pa zonsezo ndi mau onena kuti palibe woyenera kupembedzedwa mwa choonadi koma Allah ndipo yapansi penipeni ndiye kuchotsa choipa m'njira yodutsa anthu. Manyazi ndi nthambi ya chilukhulupiliro*." (Muslim).

Imaan imalimbikitsidwa ndi ntchito zabwino zomwe Msilamu amaziona mwa iye mwini, monga kuchangamuka pakumvera malamulo a Allah mu masika a Ibaadah (m'mene ilili nyengo ya mwezi wa Ramadhaan, Hajj ndi ina yotero) ndi kufooka mu nyengozo pochita zoipa. Allah akunena kuti; "*Ndithu zabwino zimachotsa zoipa*."

Ndipo nsichi zake zilipo zisanu ndi imodzi. Mneneri (SAW) anazitchula m'mau ake onena kuti: "*Umukhulupirire Allah, angero Ake, mabuku Ake, atumiki Ake,Tsiku Lomaliza, ndi chikonzero cha zabwino Zake ndi zoipa Zake*." (Bukhaari ndi Muslim).

**8 Kodi mau oti Laailaha illAllah amatanthauza chiyani?** (Mawuwa) amatanthauza kutsutsa kusayenereka kopembedzedwa wina aliyense wosakhala Allah ndi kutsimikizira kupembedzedwa kwa Allah yekha.

**9 Kodi Allah alinafe limodzi?** Inde, Allah alinafe limodzi kudzera mukuzindikira Kwake, kumva Kwake, chisamaliro Chake, kuzindikira Kwake chilichonse, mphamvu Yake ndi chifuniro Chake. Tsopano uchenicheni Wake susakanikirana ndi zolengedwa, ndipo palibe chilichonse muzolengedwa chomwe chingazindikire chili chonse cha Iye.

**10 Kodi nkutheka kuti Allah aoneke ndi diso?** Asilamu anagwirizana kuti Allah samaoneka pa dziko lapansi, ndikutinso anthu okhulupirira akamuona Allah ku Aakhirat pabwalo la msonkhano ndi ku Jannat. Allah akunena kuti: "*Nkhope zina tsiku limenelo zidzakhala zowala kwambiri, Zili kumuyang'ana Mbuye wawo*." (Surat 75: 22- 23).

**11 Kodi kudziwa maina a Allah ndi mbiri Zake kuli ndi phindu lanji?** Ndithu chilamulo choyambirira chomwe anachikhazikitsa ku zolengedwa Zake ndiko kumuzindikira Iye Allah (Subhaana Wataalaa). Choncho anthu akamuzindikira Iye adzam'pembedza moyenerera. Allah akunena kuti; "*Dziwa kuti palibe wopembedzedwa m'choonadi koma Allah, ndipo pempha chikhululuko ku zolakwa zako*" (Surat 47:49).

Choncho kukumbukira Allah pa zakuchuluka kwa chifundo Chake nkopangitsa kukhala ndi chiyembekezo. Ndipo kukhala wolanga ndi chilango chowawa n'kopangitsa kumuopa Allah. Kukhala koti Iye yekhayo ngopereka mtendere mwapadera n'kopangitsa kuyamika.

**NDIPO CHOLINGA CHA KUDZIWA MAINA A ALLAH NDI MBIRI ZAKE**:
Uko ndiko kutsimikizira kumuzindikira Iye kudzera m'maina a Allah ndi mbiri Zake muli zomwe munthu atha kuyamikidwa nazo ngati atakhala nazo, monga kuzindikira, chisoni ndi chilugamo, ndipo mwa izo muli zomwe munthu atha kudzudzulidwa ngati atadzitcha nazo, monga umulungu, kugonjetsa ndi kudzikuza. Munthu ali ndi mbiri zomwe amayamikiridwa nazo ndipo amalamulidwa kuzichita, monga kuonetsa ukapolo, umphawi,kusowa, kudzichepetsa, kupempha ndi zina zotero, koma kukuletsedwa

kutchulidwa Allah ndi mbiri zimenezi. Ndipo cholengedwa chokondedwa kwambiri kwa Allah ndi chimene chili ndi mbiri zomwe Allah amazikonda, ndipo chomwe chili choipa kwambiri kwa Iye ndi chimene chili ndi mbiri zomwe Allah amaipidwa nazo.

**12 KODI MAINA ABWINO A ALLAH NDI ATI?** Allah akunena kuti; "*Ndipo Allah ali ndi maina abwino, choncho m'pempheni ndi mainawo*"

Ndithu zatsimikizika kuchokera kwa Mtumiki (SAW) kuti iye anati; "*Ndithu Allah Wapamwambamwamba ali ndi maina makumi asanu ndi anai, mphambu zisanu ndi zinayi (99) - chikwi chimodzi kupatula limodzi-, amene angawasunge pa mtima akalowa ku Jannat*" **(Bukhaari ndi Muslim).**

**Kuwasunga mainawa muli zinthu zitatu: 1)** Kusunga mawu ake ndi chiwerengero chake. **2)** Kumvetsa matanthauzo ake zomwe akulozera ndikuwakhulupirira. Akanena kuti Al Hakeem –Wanzeru zakuya- munthuyo amagonjera zinthu zake zonse kwa Allah chifukwa zonse zimachitika malinga ndi nzeru Zake. **(3)** Kumupempha Allah kudzera m'mainawa. Mwachitsanzo anene kuti: 'Eh Inu Wobisa zonyansa ndibisireni ine! Eh Inu Wopatsa! Ndipatseniko zabwino Zanu zochuluka!' Allah wanena kuti: "*Ndipo ndininkheni ine ufumu umene siudzatheka kukhala nawo wina aliyense pambuyo panga. Ndithudi Inu ndiwoninkha*". Ndipo amene angaitsatire bwinobwino Quràn ndi Hadith yangwiro atha kuwasunga mainawa.

**MAINAWA NDI AWA:**

| DZINA | TANTHAUZO |
|---|---|
| الله<br>**Allah** | Mwini umulungu ndikupembedzedwa komwe kwakakamizidwa pa zolengedwa Zake zonse. Iye ndiwopembedzedwa amene chili chonse chimapeputsidwa pa maso Pake ndikugonjera, chimawerama ndikugwetsa nkhope zake pansi chifukwa cha Iye. Kwa Iye yekhayo ndikumene kumaperekedwa mitundu ili yonse ya Ibaadah. |
| الرحمن<br>**Al-Rahmaan** | **Wachifundo:** Ili ndi dzina losonyeza kukula kwa chifundo Chake komanso kufalikira kwa chifundocho ku zolengedwa zonse. Limenelidi ndi dzina lomwe Allah wasankhika nalo Iye yekha choncho nkosavomerezeka kumutcha nalo wina aliyense wosakhala Iye. |
| الرحيم<br>**Al-Raheeem** | **Wachisoni:** Wochitira chisoni komanso wokhululukira anthu okhulupirira pano padziko komanso pa Tsiku Lomaliza. Iye adawawongolera zoti adzimupembedza Iye ndipo akawalemekeza powapatsa Jannat Yake pa Tsiku Lomaliza. |
| العفو<br>**Al- Afuwwu** | **Wofafaniza**: Iye ndi amene amafafaniza machimo ndikuwakhululukira ndipo salanga nawo chikhalirecho kapolo anayenerera kulangidwa. |
| الغفور<br>**Al-Ghafuur** | **Wokhululuka:** Iye ndi amene amabisira tchimo mwini wake tchimolo ndipo samamuyalutsa komanso osamulanga nalo. |
| الغفار<br>**Al-Ghaffaar** | **Wokhululuka kopanda malire**: Dzina losonyeza kuchuluka kwa chikhululuko Chake kwa kapolo Wake wochimwa amene akupempha chikhululuko Chake. |
| الرؤوف<br>**Al-Rauuf** | **Woleza:** Kuchokera ku liwu loti kuleza omwe ndimapeto achisoni cholapitsa. Kulezaku nkokwanira ku zolengedwa zonse pa dziko lapansili pomwe nkosankhika kwa ena mwa iwo pa Tsiku Lomaliza. Awo ndi amene ali abwenzi Ake okhulupirira mwa Iye. |
| الحليم<br>**Al-Haleem** | **Wodekha**: Amene safulumizitsa kupereka chilango kwa akapolo Ake pamene alinako kuthekera kotero; koma amawalekerera ndi kuwakhululukira akamupempha chikhululuko. |

| | |
|---|---|
| التواب<br>**Al-Tawwaab** | **Wolandira kulapa:** Iye ndi amene amapatsa kuthekera kwa kulapa kwa akapolo Ake amene wawafuna ndikuwalandira kulapako. |
| الستير<br>**Al-Sittiir** | **Wobisa:** Iye ndi amene amaveka nsalu kapolo Wake ndipo samamuyalutsa pakati pa zolengedwa Zake. Iye ndiwokonda kuti kapolo Wake azidziveka nsalu mwini wakeyo komanso atero kwa anzake ndikutinso ayenera kumabisanso maliseche ake. |
| الغني<br>**Al-Ghaniyyu** | **Wokhupuka:** Iye sasaukira kwa wina aliyense mwa zolengedwa Zake chifukwa cha uchikwanekwane Wake ndi kukwanira kwa mbiri Zake. Zolengedwa zonse zimasowa thangato Lake komanso zimasaukira ku zopatsa Zake komanso chithandizo Chake. |
| الكريم<br>**Al-Kareem** | **Wopatsa**: Iye ndi mwini zabwino zambiri ndipo woninkha kwambiri ndikupatsa. Amapereka zimene akufuna kwa amene akumufuna m'menenso angafunire kaya kudzera pomupempha pena ayi. Iye amakhululuka machimo komanso amabisa zinthu zochititsa manyazi. |
| الأكرم<br>**Al-Akram** | **Wamituka:** Amene wafika mapeto amituka. Alibe wofanana naye pa zimenezi mpaka kalekale. Zabwino zonse zimachokera kwa Iye. Adzawalipira anthu okhulupirira ndi zabwino Zake komanso amadekhera anthu otsutsana Naye ndipo adzawawerengera ntchito zawo mwachilungamo Chake. |
| الوهاب<br>**Al-Wahhaab** | **Woninkha**: Amapereka ndikuninkha kwambiri kopanda chosinthana nacho. Amaperekanso popanda cholinga china chomwe chingabwerere kwa Iye. Ndipo amapereka mtendere popanda kupempha. |
| الجواد<br>**Al-Jawwaadu** | **Mataya**: Wochulukitsa popereka zabwino ndi ubwino kwa akapolo Ake onse. Ndipo amene amakhulupirira Iye adzapeza gawo lalikulu kwambiri la mituka Yake komanso ubwino Wake. |
| الودود<br>**Al-Waduud** | **Wachikondi chopanda malire**: Amakonda abwenzi Ake ndipo amawakondetsetsa powapatsa chikhululuko ndi mtendere kotero amawasangalalira ndikumawalandira ntchito zawo zabwino ndikuwachita iwo kukhala ovomerezedwa pa dziko. |
| المعطي<br>**Al-Mu'utwii** | **Wopereka**: Amapereka chili chonse chimene wafuna kwa amene wamufuna mu zolengedwa Zake kuchokera mu nkhokwe Zake. Tsono abwenzi Ake, ali nalo gawo lokwanira mu zopatsa Zakezo. Iye ndi amene adapereka kwa chinthu chili chonse chilengedwe chake komanso maonekedwe ake. |
| الواسع<br>**Al-Waasi'i** | **Wachikwanekwane:** Iye ndi mwini mbiri zabwino zochuluka ndipo sangakwaniritse wina aliyense kumutamanda. Wachikwanekwane pa ukulu komanso ufumu Wake. Wochulukitsa chikhululuko komanso chisoni. Wa ubwino wopanda malire komanso wa zabwino zonse. |
| المحسن<br>**Al-Muhsin** | **Wabwino:** Iye mwa Iye Yekha ali nawo ubwino komanso mu maina Ake, mbiri Zake ndinso zochita Zake. Iye adalenga chinthu chili chonse mwachilengedwe chabwino ndipo amachitira zabwino zolengedwa Zake. |
| الرازق<br>**Al-Raaziq** | **Wopereka zosoweka zaumoyo:** Iye ndi amene amapereka rizq (zosoweka za umoyo) kwa zolengedwa zonse. Ndipo adaika dongosolo lonse la rizq la zolengedwazi asadazilenge. Komanso Iye ndiwosunga pokwaniritsa kuti aliyense apeze gawo lake la rizq angakhale patadutsa nthawi yotani. |
| الرزاق<br>**Al-Razzaaq** | Ili ndi dzina losonyeza kuchuluka kwa rizq Lake pa zolengedwa Zake. Iye –Subhaana Wataalaa- amazipatsa zolengedwa Zake rizq zisadamupemphe. Ndiponso amazipatsa zosoweka za moyo wawo angakhale zikumamulakwira. |

| | |
|---|---|
| اللطِيف<br>**Al-Latweef** | **Wodziwitsitsa:** Iye ndiwodziwitsitsa zinthu zingachepe maka moti palibe kangabisike kwa Iye. Amafikitsa zabwino ndi mathandizo kwa akapolo Ake mu njira zobisika kuchokera komwe samayembekezera. |
| الخبير<br>**Al-Khabeer** | **Wozindikira:** Iye ndi amene kuzindikira Kwake kwazungulira pozidziwa zinthu zobisika mofanana ndi umo amazidziwira zinthu zowonekera. |
| الفتاح<br>**Al-Fattaah** | **Wotsegula:** Iye ndi amene amatsegula kuchokera mu nkhokwe za ufumu Wake, chifundo Chake ndi rizq Lake m'mene angafunire mofanana m'mene chikonzero Chake ndi kuzindikira Kwake kulili. |
| العليم<br>**Al-Aleem** | **Wodziwa**: Iye ndi amene kuzindikira Kwake kwazungulira pa zinthu zowonekera, zobisika, zachinsinsi, zolengezera poyera, zakale, zalero komanso zamtsogolo. Palibe mu zinthu zonse kanthu kalikonse kangabisike kwa Iye. |
| البر<br>**Al-Barru** | **Wabwino**: Iye ndiwochulukitsa ndi zabwino Zake ku zolengedwa. Amapatsa moti nkosatheka wina aliyense kuwerengetsera mtendere Wake. Iye ndiwoona mtima pa lonjezo Lake, yemwe amakhululukira kapolo Wake, kumuteteza ndikumuchengetera komanso amalandira chochepa kuchokera kwa iye nachichulukitsa. |
| الحكيم<br>**Al-Hakeem** | **Wolinganiza bwino**: Iye ndi amene amaika chili chonse m'malo mwake moyenera ndipo mukulinganiza Kwake simulowamo kuonongeka kuli konse ngakhalenso kuchepekedwera. |
| الحكم<br>**Al-Hakam** | **Muweluzi:** Iye ndi amene adzaweluze pakati pa zolengedwa Zake mwachilungamo. Kotero Iye sakapondereza aliyense mwa iwo. Iye ndi amene adavumbulutsa Buku Lake Lapamwamba kuti likhale muweluzi pakati pa anthu. |
| الشاكر<br>**Al-Shaakir** | **Wothokoza:** Amayamikira amene akumvera malamulo Ake namamutamanda. Iye amalipira ntchito ili yonse ingachepe maka. Iye amakumana kuthokoza kwa akapolo Ake pano pa dziko powawonjezera zabwino ndi kuwapatsa malipiro Tsiku Lomaliza. |
| الشكور<br>**Al-Shakuur** | **Woyamika**: Ntchito zochepa za akapolo Ake kwa Iye zimakhululukidwa ndikuwaonjezera nazo malipiro. Kuyamika kwa Allah pa kapolo Wake ndiko kupereka malipiro Ake kapoloyo akayamika ndikulandira ntchito zake zabwino kuchokera kwa iye. |
| الجميل<br>**Al-Jamiil** | **Wokongola:** Iye mwa Iye Yekha ndiwokongola komanso mu maina Ake, mbiri Zake ndi zochita Zake muli kukongola kopanda malire. Kukongola kulikonse kopezeka pa zolengedwa Zake kumachokera kwa Iye. Wayeretsedwa Iye ndiponso wapamwambamwamba. |
| المجيد<br>**Al-Majeed** | **Waulemerero**: Iye ndi Amene ali nako kuthimbwidzika, kupatsa ulemerero, upamwamba ku mitambo yonse komanso pa dziko pano. |
| الولي<br>**Al-Waliyyu** | **Muimiriri**: Iye ndi muimiriri pa zinthu zonse zokhudzana ndi zolengedwa Zake ndi polondoloza ndondomeko ya ufumu Wake. Iye ndi mtetezi komanso mthangati wa abwenzi Ake. |
| الحميد<br>**Al-Hameed** | **Wotamandika:** Iye ndowotamandika pa maina Ake, mbiri Zake ndi zochita Zake. Iye ndi amene amatamandidwa pa chisangalalo, pa mavuto, pa mikwingwirima komanso pa mtendere. Iye ndiwoyenerera kutamandidwa ndikutchulidwa ndi mbiri zabwino mapeto otero chifukwa Iye ndi amene amatchuka ndikukwanirira konse. |
| المولى<br>**Al-Maulaa** | **Bwana**: Iye ndi mleri, mfumu, bwana,mtetezi ndi mthangati wa abwenzi Ake. |

| | |
|---|---|
| النصير<br>**Al-Nasweer** | **Muwomboli:** Iye ndi amene amathandiza amene akumufuna kudzera mu uwomboli Wake. Palibe angagonjetse yemwe Iye wamuwombola komanso palibe angamuombole amene wamulekerera. |
| السميع<br>**Al-Sami'i** | **Wakumva:** Iye ndi amene kumva Kwake kwazungulira kumva chili chonse chobisika, manong'onong'o, zolimbika, zolengeza kungoti amamva mawu aliwonse angachepe kapena kukula motani. Iye amayankha amene wamupempha. |
| البصير<br>**Al-Basweer** | **Woyang'ana**: Iye ndi amene kuyang'ana Kwake kwazungulira kuwona zonse zopezeka kaya m'dziko la zobisika zosawoneka ndi maso komanso zoonekera. Zingabisike motani kapena kuonekera komanso zingachepe maka kapena kukula- Iye amaziona basi. |
| الشهيد<br>**Al-Shaheed** | **Woikira umboni**: Iye ndi muayang'aniri wa zolengedwa Zake. Anadziikira umboni Yekha pa za umodzi Wake komanso zochita chilungamo. Iye amachitira umboni kuona mtima kwa anthu okhulupirira akamatchula umodzi Wake. Ndipo Iye amachitira umboni atumiki Ake kudzanso angero. |
| الرقيب<br>**Al-Raqeeb** | **Muyang'aniri**: Iye ndi amene amayang'anira zonse zochitika za zolengedwa Zake. Komanso Iye ndi amene amawerengera ntchito za zolengedwa Zake zonse moti sikungamudutse kutembenuka kwa woyang'ana kapena kanthu kodutsa m'maganizo. |
| الرفيق<br>**Al-Rafeeq** | **Wodekha**: Iye ndiwochulukitsa kudekha pa zochita Zake. Iye –Subhaanahu Wataalaa- amachita modekha ndi mwapang'onopang'ono pa malamulo Ake pa zolengedwa Zake. Iye amakhalira kuchitira akapolo Ake zinthu modekha ndi mofatsa moti sawakakamiza kuchita zinthu zoposera kuthekera kwawo. Iye Subhaanahu Wataalaa amakonda akapolo Ake amene ali odekha. |
| القريب<br>**Al-Qareeb** | **Wapafupi**: Iye ali pafupi mwakuzindikira Kwake ndikuthekera Kwake pa zolengedwa Zake zonse. Ndipo Iye ali pafupi ndi chifundo Chake, chitetezo Chake kwa akapolo okhulupirira. Iyeyo ngakhale zili dero ali pamwamba pa mpando Wake waulemerero ndipo chenicheni cha Iye sichisakanikirana ndi zolengedwa. |
| المجيب<br>**Al-Mujeeb** | **Woyankha**: Iye ndi amene amayankha kuitana kwa woitana komanso pempho la wopempha. |
| المقيت<br>**Al-Muqiitu** | **Wodyetsa**: Iye ndi amene adalenga zakudya zonse zomwe zolengedwa zimadalira komanso marizq- zosoweka zonse za umoyo ndipo Iye ndimwini kufikitsa zimenezi kwa zolengedwa. Iye ndi msungi wa zonsezi komanso msungi wa ntchito za akapolo popanda kupunguza. |
| الحسيب<br>**Al-Haseeb** | **Wowerengera**: Iye ndi wowakwaniritsira akapolo Ake ku zinthu zonse zimene zawavuta pa chipembedzo chawo komanso za pa dziko. Tsono anthu omukhulupirira Iye amakhala nalo gawo lalikulu la chisamaliro Chakecho. Iye - Subhaanahu Wataalaa - ndi amene ati adzawawerengere iwowo zimene adachita pa dziko lapansi. |
| المؤمن<br>**Al-Mu'umin** | **Wopatsa mtendere**: Iye ndi amene amavomereza atumiki ndi owatsatira awo powaikira umboni zakunena zoona kwawo. Komanso ndi maumboni amene amaonetsera osonyeza kuona kwawo. Komanso mtendere uliwonse umene uli pa dziko pano komanso Tsiku Lomaliza, Iye ndi amene amapatsa. Iye ndi mtetezi wa anthu amene amamukhulupirira kuti asadzawapondereze, asadzawalange kapena kuwapatsa kutekeseka kwa tsiku la Kiyama. |
| المنان<br>**Al-Mannaan** | **Wopatsa mowirikiza:** Iye ndiwopatsa zambiri, wopereka mtendere waukulu, wochulukitsa kuchitira zabwino zolengedwa Zake. |

| | |
|---|---|
| الطيب<br>**Al-Twayyib** | **Wabwino:** Iye ndi woyera ndipo wopanda chilema chili chonse kapena kupunguka kwina kuli konse. Iye ndi amene ali nawo ubwino uli wonse komanso kukwanirira kopanda malire. Iye ali nazo zabwino zambiri zozipatsa zolengedwa Zake ndipo salandira-Subhaanahu Wataalaa- ntchito zili zonse kapena sadaka iliyonse kupatula zimene zili zabwino za halaal komanso zokhazo zimene alungamika nazo kwa Iye- zoyera. |
| الشافي<br>**Al-Shaafi** | **Wochiza:** Amene amachiza matenda a m'mitima ndi matupi. M'manja mwa akapolo mulibe kuthekera kulikonse- kupatula zomwe Allah wawafewetsera mu gawo la mankhwala. Tsono kuchiza ndiye kuli m'manja Mwake Iye yekhayo basi. |
| الحفيظ<br>**Al-Hafeez** | **Msungi:** Iye ndi Amene amasunga ndikuchengetera akapolo Ake okhulupirira ndi ntchito zawo kudzera mu ubwino Wake. Iye amazisamalira ndi kuzisunga zolengedwa zonse kudzera mukuthekera Kwake**.** |
| الوكيل<br>**Al-Wakeel** | **Wosamalira:** Iye ndi Amene amayang'anira zolengedwa zonse. Ndipo Iye wazisamalira pozilenga ndi polinganiza bwino chili chonse chokhudzana nacho. Iye ndi Amene amadaliridwa ndi zolengedwa Zake pochititsa kuti zipezeke zamoyo ndiponso kuzininkha zosoweka zake. Iye ndi msungi wa anthu okhulupirira amene atsogoza chigonjero cha zinthu zonse kwa Iye asanagwire ntchito zawo, namapempha chithandizo Chake pa nthawi imene akugwira ntchito zawo, namatamanda Iye pothokoza pambuyo poti awapatsa kuthekera kotero komanso namakhuthira gawo limene agawiridwa pambuyo powapatsa mayeserero. |
| الخلاق<br>**Al-Khallaaq** | **Mlengi**: Dzina losonyeza kuchuluka kwa zinthu zomwe Allah amalenga. Iye –Subhaanahu Wataalaa- sadaleke akulengabe ndipo sadzaleka kukhala ndi mbiri yaikulu imeneyi mpaka kalekale. |
| الخالق<br>**Al-Khaaliq** | **Mlengi:** Iye ndi Amene adalenga zolengedwa zonse kopanda kotengera kapena pofananizira ndi pena pake m'mbuyomu ayi. |
| البارئ<br>**Al-Baariu** | **Muyambitsi**: Iye ndi Amene adachititsa kuti zinthu zimene adaziringaniza zipezeke ndi kuzivomereza zolengedwa zonse nazitulutsirano poyera kuti zipezeke. |
| المصور<br>**Al-Muswawwir** | **Mlengi wamaonekedwe**: Iye ndi Amene anachititsa kuti zolengedwa Zake zikhale m'maonekedwe amene Iye adawasankha, malinga ndi nzeru Zake zakuya, kuzindikira Kwake ndi chifundo Chake. |
| الرب<br>**Al-Rabb** | **Mleri:** Iye ndi Amene amalera zolengedwa Zake kudzera mu zabwino Zake ndikumazikuza pang'onopang'ono. Iye ndi Amene amalera abwenzi Ake ndi zinthu zimene zingakonze mitima yawo. Iye ndi mlengi, mwini zonse komanso bwana. |
| العظيم<br>**Al-Adheem** | **Wamkulu**: Iye ndi Amene ali ndi ukulu wonse wopanda malire mu uchenicheni Wake, m'maina Ake komanso mbiri Zake. Pachifukwa ichi kwakhala kokakamizidwa kwa zolengedwa zonse kuti zidzimukuza Iye ndi kumulemekeza ndikukuza malamulo Ake komanso zimene waletsa. |
| القاهر<br>**Al-Qaahir** | **Wogonjetsa**: Iye ndi Amene amapeputsa akapolo Ake, amazichititsa zolengedwazo kukhala akapolo Ake, ali pamwambamwamba pa zonsezo. Iye ndiwopambana komanso wogonjetsa ndipo Iye ndi Amene makosi ndi nkhope zonse zagonjera mwa Iye. |
| القهار<br>**Al-Qahhaar** | **Wogonjetsa molapitsa**: Ili ndi dzina losonyeza kupyoza malire pa chigonjetso kuposa kunena kuti AlQaahir. |
| المهيمن<br>**Al-Muhaimin** | **Wosamalira**: Iye ndi Amene amasamalira chinthu chili chonse ndipo ndi msungi wake. Iye amachiona chili chonsecho komanso amachizungulira mbali zonse. |

| | |
|---|---|
| العزيز<br>Al-Ázeez | **Wopambana:** Iye ali nawo matanthauzo akupambana aliwonsewo. Kupambana kokhala ndi nyonga moti palibe angagonjetse Iye. Kupambana kodzikhuthira moti sangasowekerenso thandizo la wina aliyense. Kupambana kogonjetsa moti palibe chimene chingatekeseke kupatula mu chifuniro Chake basi. |
| الجبار<br>Al-Jabbaar | **Wodzikweza**: Iye ndi Amene ali ndi chifuniro cha chochitika. Zolengedwa zonse ndi zogonjetsedwa kwa Iye komanso zagonjera ukulu Wake. Zonse zimayendetsedwa malinga ndi nzeru Zake. Iye ndi Amene amaluzanitsa zosweka, kulemeretsa wosauka, kufewetsa zovuta ndikutonthoza wodwala komanso amene ali m'mavuto. |
| المتكبر<br>Al-Mutakabbir | **Wodzikweza**: Iye ndi wamkulu,wodzikweza, wopanda koipa kalikonse ngakhalenso kupunguka. Iye wodzitukumula woti sangapondereze akapolo Ake. Iye ndi mgonjetsi kwa zolengedwa Zake zamakani. Iye ndi wotchuka ndi kudzikweza ndipo amene angapikisane naye pofuna kukhala ngati Iye pa zimenezi amamuswa ndikumulanga. |
| الكبير<br>Al-Kabeer | **Wamkulu:** Iye ndi wamkulu mu uchenicheni Wake ndi mu mbiri Zake komanso ntchito Zake. Palibe china chili chonse chomwe chingakhalepo choposa Iye. M'malo mwake china chili chonse chosakhala Iye ndi chaching'ono pamaso pa ulamuliro ndi ukulu Wake. |
| الحيي<br>Al-Hayiyy | **Wamanyazi**: Iye ndi Amene ali ndi manyazi woyenerera ndi kulemekezeka kwa nkhope Yake ndi ukulu wa ufumu wake.Ndiye manyazi a Allah ndi manyazi a kulemekezeka, ubwino, kupatsa komanso ulemerero. |
| الحي<br>Al-Hayy | **Wamoyo**: Iye ndi Amene ali nawo moyo wosatha wamuyaya. Umuyaya wopanda chiyambi kapena mathero. Ndiye moyo uli wonse umene ukupezeka pa dziko ndithudi umenewo ukuchokera kwa Iye Subhaanahu Wataalaa. |
| القيوم<br>Al-Qayyuum | **Wodzidalira**: Iye ndi wodziimira payekha ndipo ngosadalira pazolengedwa Zake. Iye ndi Amene amachetengera china chili chonse chomwe chili ku mitambo komanso pa dziko lapansili onsewo amasaukira Iye. |
| الوارث<br>Al-Waarith | **Mulowam'malo wazonse:** Iye yekhayo ndi wotsala pambuyo pakutha zolengedwa Zake. Zinthu zonse pambuyo pakutha eni ake,zidzabwerera kwa Iye. Zonse zimene zili m'manja mwathu ndi amaanat tsiku lina zidzabwerera kwa mwini wake weniweni Allah Subhaanahu Wataalaa. |
| الديان<br>Al-Dayyaan | **Muweluzi:** Iye ndi Amene zolengedwa zonse zagonjera mwa Iye komanso zadzichepetsa. Iye ndi Amene adzalipire akapolo Ake pazomwe adachita. Ngati adachita chabwino ndiye kuti akachionjezera koma ngati chili choipa ndiye kuti akamulanga nacho kapena kumukhululukira. |
| الملك<br>Al-Malik | **Mfumu**: Iye ndi Amene ali nawo ulamuliro, mphamvu yoletsa zinthu zoipa komanso kupambana. Iye ndi Amene ali ndi chifuniro chochita pazolengedwa Zake kudzera mu lamulo Lake kapena zochita Zake. Palibe aliyense amene ali ndi ubwino wothandizira kuti ufumu Wake ukhazikike kapena kuwusamalira. |
| المالك<br>Al-Máalik | **Mwini zonse:** Ufumu Wake ndi wapaphata komanso woyenerera. Ufumu udali wake panthawi imene amalenga zolengedwa kotero padalibe wina amene adali nawo koma Iye yekhayo. Komanso ufumu udzakhalabe wakewake panthawi yochoka ndikutha zolengedwa zonse. |
| المليك<br>Al-Maleek | Ili ndi dzina losonyeza mbiri ya ulamuliro Wake wopanda malire. Dzinali ndi la matanthauzo ozama kuposa loti Al-Malik. |
| السبوح<br>Al-Subbuuh | **Woyeretsedwa:** Iye ndi woyeretsedwa ku chilema chili chonse komanso kupunguka chifukwa choti mbiri ya uchikwanekwane ndi kukongola kopanda malire ndikwake. |

| | |
|---|---|
| القدوس Al-Qudduus | **Woyera**: Iye ndi woyeretsedwa komanso kutalikitsidwa kukupunguka kapena chilema mwa njira ina ili yonse. Zili dero chifukwa Iyeyo ndi wosankhika pa umodzi Wake pokhala ndi mbiri za uchikwanekwane wopanda malire kotero sipangaikidwe pa Iye zifananizo. |
| السلام Al-Salaam | Iye ali nako kutali kuperewera komanso chilema pa uchenicheni Wake kapena mu mbiri Zake ndi zochita Zake. Komanso bata ndi mtendere uliwonse umene ukupezeka pa dziko lapansili komanso Tsiku Lomaliza ndiye kuti ukuchokera kwa Iye Subhaanahu Wataalaa. |
| الحق Al-Haqq | **Choonanadi**: Iye ndi Amene mwa Iye mulibe chipeneko chili chonse komanso chikaiko.Mu maina Akenso komanso mbiri zake mulibemo chikaiko chimodzimodzinso mu umulungu Wake. Iye ndiwopembedzedwa mu choonadi. Palibe angapembedzedwe mwachoonadi kupatula Iye. |
| المبِين Al-Mubeen | **Wapoyera**: Iyeyo zinthu Zake ndi zoonekera poyera mu umodzi Wake, luntha Lake komanso chifuniro Chake. Iye ndi Amene amalongosolera akapolo Ake njira za chisokezo kuti azipewe. |
| القوي Al-Qawiyyu | **Wanyonga:** Iye ndi Amene ali nako kuthekera kopanda malire pamodzi ndi uchikwanekwane pachifuniro. |
| المتين Al-Mateen | **Wolimba-Wamphamvu**: Iye ndi wolimba kwambiri mu mphamvu Zake ndi kuthekera Kwake. Palibe chopweteka chili chonse chingam'peze mu zochita Zake kapena vuto lili lonse ngakhalenso kutopa kumene. |
| القادر Al-Qaadir | **Wakuthekera**: Iye ali nako kuthekera pa chinthu chili chonse ndiye palibe chimene chingamukanike pa dziko lapansili ngakhalenso ku mitambo. Iye ndiye mkonzi wachinthu chili chonse. |
| القدير Al-Qadeer | Ili ndi dzina lotanthauzanso Al-Qaadir –Wakuthekera- kupatula kuti lili ndi matanthauzo ozama kuposa Al-Qaadir**.** |
| المقتدر Al-Muqtadir | Dzina losonyeza tanthauzo lakuya mu kuthekera kwa AllahTaalaa pokwaniritsa zilinganizo zonse ndikuzilenga pa zomwe zafika zimene zatsogola mu kuzindikira kwa Allah. |
| العلي Al-Aliyy الأعلى Al-Aalaa | **Wapamwamba**: Iye ndi Amene zinthu Zake ndi zopambana komanso umwini ndi uchenicheni Wake ndi wopambana. Chinthu chili chonse chili pansi pa mphamvu Zake ndinso ufumu Wake. Palibe china chimene chingakhale pamwamba pake mpaka kalekale. |
| المتعال Al-Muta'alee | **Wodzitukula**: Iye ndi Amene pamaso pa kutukuka Kwake chili chonse chapeputsidwa. Palibe chimene chingakhale pamwamba Pake mpaka kalekale koma chili chonsecho chili pansi Pake ndi pansi pa mphamvu Zake komanso ufumu Wake. |
| المقدم Al-Muqaddir | **Wotsogoza:** Iye ndi Amene amatsogoza zinthu ndikuziika m'malo ake oyenerera ndi chifuniro chake ndi luntha Lake. Ndipo amatsogoza zina mwa zolengedwa Zake pamwamba pa zina mofanana ndi kuzindikira Kwake ndi ubwino Wake. |
| المؤخر Al-Muakhir | **Wobweza m'mbuyo**: Iye ndi Amene amaika zinthu m'malo mwake, amatsogoza zimene wazifuna ndikuzibwezera m'mbuyo zimene wazifuna kudzera mu luntha Lake. Amachedwetsa chilango kwa akapolo Ake kuti mwina alape ndikubwerera kwa Iye. |
| المسعر Al-Musai'ir | **Woika mitengo**: Iye ndi amene amaonjezera mitengo ya zinthu ndi kufunika kwake pakati pa anthu ndi zimene zingachite; kapena kuzipeputsa ndikuzitsitsa, motero zinthu nkumakwera mitengo kapena kutsika mofanana ndi m'mene luntha Lake lilili komanso kuzindikira Kwake. |

| | |
|---|---|
| القابض<br>Al-Qaabidh | **Wofumbata**: Iye ndi Amene amafumbata mitima yonse. Iye ndi Amenenso amagwira - osapereka - marizq kwa amene wamufuna mu zolengedwa Zake kudzera mu luntha Lake ndi kuthekera Kwake cholinga chowayesa mayeso iwowo. |
| الباسط<br>Al-Baasit | **Wotambasula:** Iye ndi Amene amachulukitsa rizq akapolo Ake ndi mituka Yake komanso chifundo Chake. Kenako amayesa nazo zimenezo mofanana ndi luntha Lake. Komanso amatambasula manja Ake kulandira kulapa kwa amene anasakaza. |
| الأول<br>Al-Awwal | **Woyamba**: Iye ndi Amene padalibe china chili chonse patsogolo Pake. Koma kuti zolengedwa zonse zidapezeka pakulenga Kwake kwa zimenezo. Tsono Iye Subhaaanahu Wataalaa ndiye alibe chiyambi chakupezeka Kwake. |
| الآخر<br>Al-Aakhir | **Womaliza:** Iye ndi Amene palibe chinthu chili chonse pambuyo Pake. Iye ndiwotsala panthawi imene chili chonse chimene chili pa dzikopa chidzathe kenako mabwerero awo ndi kwa Iye. Alibenso mathero akupezeka Kwake-Allah. |
| الظاهر<br>Al-Dhaahir | **Wowoneka**: Iye ndi wotukuka pamwamba pa chinthu china chili chonse. Palibe chinthu chimene chili chotukuka kuposa Iye. Iye ndi mgonjetsi wachinthu china chili chonse ndipo wachizingulira kuchidziwa bwino. |
| الباطن<br>Al-Baatwin | **Wobisika**: Iye ndi Amene palibe kanthu kena kake pansi Pake kangabisike. Iye ndi wapafupi, wochizungulira chinthu chili chonse mbali zonse kuchidziwa ndi kuchiona koma Iyeyo ngobisika ku maso azolengedwa zonse pano pa dziko lapansili -sizingamuone. |
| الوتر<br>Al-Witr | **Wopanda chinzake:** Iye ndi mmodzi Amene alibe mthandizi. Komanso wayekhayekha Amene alibe wofanana naye. |
| السيد<br>Al-Sayyid | **Bwana**: Iye ndi Amene ali nawo ubwana wopanda malire pa zolengedwa Zake komanso akapolo Ake. |
| الصمد<br>Al-Samadu | **Woadalirika**: Iye ndi bwana Amene wakwanira ubwana Wake. Iye ndi amene zolengedwa zonse zimayang'ana maso kwa Iye pa zilakolako zawo zonse chifukwa chokula kusaukira kwawo kwa Iye-Allah. Iye ndi Amene amadyetsa ndipo sadyetsedwa. |
| الواحد<br>Al-Waahid<br>الأحد<br>Al-Ahad | **Wayekhayekha:** Iye ndi Amene ali wayekhayekha ndi uchikwanekwane onse wopanda malire moti palibe aliyense amene amathandizana mu zimenezo. Alibe wofanana Naye. Izi zikulimbikitsa kumuchitira Iye yekhayo pomupembedza popanda wothandizana kapena kusakanikirana Naye. |
| الإله<br>Al-Ilaahu | **Wopembedzedwa**: Iye ndi wopembedzedwa mwachoonadi. Iye ndi woyenerera kupembedzedwa yekhayo basi osati wina aliyense osakhala Iye. |

**13 KODI PAKATI PA MAINA A ALLAH NDI MBIRI ZAKE PALI KUSIYANA KWANJI?** Maina a Allah ndi mbiri Zake akugwirizana pakuloledwa kudzitchinjirizira ndi kulumbira kudzera m'maina ndi mbirizo. Koma pakati pake pali kusiyana kungapo ndipo kusiyana kwake kwakukulu koyamba ndi uku:

**1)** Kuloledwa popembedza komanso kupempha ndi maina a Allah ndi mbiri Zake komanso kutchulidwa dzina loti kapolo wa..(mumaina Ake). Ndiye kutchulidwa dzina loti: Abdul Kareem (kapolo wa Wolemekezeka) nkololedwa pamene dzina loti Abdul Karam (kapolo wa Wamituka yomwe ndi mbiri ya Allah) nkosaloledwa, ndipo kupempha monga kunena kuti: Yaa Kareem! nkoleledwa pamene sizikuloledwa kunena kuti: Yaa Karam- Allah!

**2)** Kusiyana kwachiwiri ndi koti mbiri zimachokera m'maina a Allah, monga mbiri ya chisoni imachokera mudzina loti *Al- Rahmaan*, tsopano maina Ake sachokera mu

mbiri, zimenezo sizinadze mu Hadith. Choncho mbiri yoti ISTIWAAU kukhazikika (pa chimpando cha ufumu Wake) simutulukamo dzina loti Mustawiyy- Wokhazikika.
**3)** Kusiyana kwachitatu ndi koti maina a Allah satuluka mu zochita za Allah zomwe mu Hadith mulibe. Choncho mu Ghadhwab - mkwiyo - motero sizinganenedwe kuti Ghaadhwib -wamkwiyo- kukhala limodzi mwa maina a Allah. Tsopano mbiri Zake zimatuluka kuchokera mu zochita Zake, motero mbiri ya mkwiyo tikum'patsa Allah chifukwa kukwiya ndi chimodzi mwa zochita Zake.
**14 Kodi kuwakhulupirira angero kumatanthauza chiyani?** Kumeneko ndiko kuvomera kotsimikiza kupezeka kwao ndi kuti Allah (SW) anawalenga kuti azimpembedza Iye ndi kukwaniritsa lamulo Lake, Allah akunena kuti: "*Amenewo ndi akapolo olemekezeka, samutsogolera Iye ndi mau ndipo iwo amagwiritsira ntchito chilamulo Chake*".

**Ndipo kuwakhulupirira iwo mkati mwake muli zinthu izi: 1)** Kukhulupirira kupezeka kwao. **2)** Kumukhulupirira amene tamudziwa dzina lake, wina mwa iwo ndi Jibril. **3)** Kukhulupirira zomwe tazidziwa mu mbiri zawo, monga kukula kwa kalengedwe kawo. **4)** Kukhulupirira ntchito zao zomwe tazidziwa zomwe anapatsidwa monga MALAKULMAUT- mngero wa imfa.
**15 Kodi Quràn ndi chiyani?** Quràn ndi mau a Allah, yomwe kuiwerenga kwake ndi ibaadat, inayambira kwa Iye idzabwereranso kwa Iye, anaiyankhula mwa choonadi pa chilembo komanso liwu, Jibril (AS) anaimva kuchokera kwa Iye, kenako Jibril (AS) anaifikitsa kwa Mneneri Muhammad (SAW). Ndipo Mabuku onse a kumwamba ndi mau a Allah .
**16 Kodi tikhutitsidwe ndi Quràn yokha ndikusiya Sunnat ya Mneneri (SAW)?** Sizikuloledwa, pakuti Allah (SW) analamula kugwiritsa ntchito Sunnat m'mau Ake (SW) onena kuti: "*Ndipo chimene wakupatsani Mtumiki chilandireni ndipo chimene wakuletsani chisiyeni*." **(Surat 59:7)**. Sunnat inadza kukhala yomasulira Quràn, ndipo tsatanetsatane la deen silingadziwike pokhapokha ndi sunnat. Mwachitsanzo Swalaat, ndondomeko yake itha kudziwika bwino ndi sunnat'yo. Mtumiki (SAW) anati: "*Imvani! Ine ndapatsidwa Quràn limodzi ndi chofanana ndi iyo, imvani! Akuyandikira munthu amene wakhuta atakhala pampando wake kuyankhula kuti muyenera kutsatira Quràn iyi, choncho cha Halaal chimene mwachipeza m'menemu chichiteni kukhala cha Halaal, ndipo cha Haraam chimene mwachipeza m'menemu chichiteni kukhala cha Haraam*." **(Abu Dawood).**
**17 Kodi kuwakhulupirira atumiki kukutanthauza chiyani?** Kumeneko ndiko kuvomera kotsimikiza kuti Allah (SW) anatumiza ku ummat ulionse Mtumiki wochokera mwa iwo, amaitanira kuti ampembedze Allah Yekha, ndikuzikana zomwe zikupembedzedwa zosakhalaAllah, ndikutinso onsewo ndi onena zoona, ovomerezedwa, owongoka, olemekezeka, abwino, omuopa Allah, okhulupirika, awongoli, otsogoleredwa ndikutinso iwo anafikitsa uthenga wawo, ndikutinso iwo ndi abwino kwambiri mu zolengedwa, ndikutinso iwo ndi otalikitsidwa ku Shirk kuyambira kubadwa mpaka ku mwalira kwao.
**18 Ndi mitundu yanji ya Duà yomwe idzakhale pa tsiku la Kiyaamat? 1)** Pali mitundu ingapo ya ma Duàa, Duàa yaikulu mwa ma Duaàwa imeneyo ndi Duàa

yomwe idzakachitidwe pa Bwalo la Kiyaamat pambuyo poti anthu atangoimirira kokwana zaka zikwi makumi asanu akudikirira kuti milandu yawo igamulidwe, choncho Mneneri Muhammad (SAW) adzachita Duàa kwa Mbuye wake, ndipo adzam'pempha kuti agamule pakati pa anthu ndipo Duàa imeneyo wasankhika nayo yekhayo Bwana wathu Muhammad (SAW) mwa ma ummat onse amenewo ndi malo woyamikika amene iye adalonjezedwa. **2)** Duwa yopempha kuti khomo la Jannat litsegulidwe ndipo woyamba amene khomo lake lidzatseguliridwe ndi Mtumiki wathu Muhammad (SAW) komanso ummat woyamba kulowa ku Jannat udzakhala ummat wake (SAW). **3)** Mtundu wachitatu ndi Duàa yowachitira anthu omwe alamulidwa kuti akalowe ku moto kuti asakaloweko. **4)** Mtundu wachinayi ndi Duàa yowachitira anthu amene akalowe ku moto omwe anali Asilamu onyozera malamulo kuti akatulutsidwe ku motoko. **5)** Mtundu wachisanu: iyi ndi Duàa yowakwezera anthu ma ulemelero mwa anthu aku Jannat. **6)** Mtundu wachisanu ndi chimodzi: iyi ndi Duàa yodzawachitira anthu ena kuti akalowe ku Jannat mopanda chiwerengero. **7)** Mtundu wachisanu ndi chiwiri: iyi ndi Duàa yowapeputsira chilango makafiri ena, ndipo Duàa imeneyi ndi ya Mneneri wathu yekha Muhammad (SAW) yomwe akawapemphere amalume ake Abu Twaalib kuti chilango chawo chikapeputsidwe. **8)** Kenako Allah (SW) ndi chifundo Chake adzakatulutsa ku moto anthu ena omwe adamwalira akukhulupirira umodzi wa Allah popanda Duàa ya wina aliyense, palibe amene akudziwa chiwerengero chao koma Allah, ndipo akalowetsa ku Jannat mwa chifundo Chake.

**19 Kodi n'zololedwa kupempha chithandizo kapena Duàa kwa anthu amoyo?**

Inde nzololedwa, ndipo ndithu shariat yalimbikitsa za kum'thandiza wina, motero Allah Ta'ala akunena kuti: "*Ndipo thandizanani pa zinthu zabwino ndi zomuopa Allah*" **(Surat 5: 2)**. Ndipo Mtumiki (SAW) anati: "*Ndipo Allah amamuthandiza munthu ngati munthuyo amamuthandiza m'bale wake*." **(Muslim)**. Tsopano shafa-at (Dua'a) ubwino wake ndi waukulu, ndipo shafa-at imeneyi ikutanthauza kuti pempho lodzera mwa munthu wina, pakuti Allah wanena kuti: "*Amene angampempherere mnzake pempho labwino adzapeza gawo m'menemo*." **(Surat 4:85)**. Ndipo Mtumiki (SAW) anati: "*Apemphererení ena m'zofuna zawo mudzalipidwa*." **(Bukhaari)**

**Ndipo zonsezo kuti zitheke pali zinthu zingapo zofunikira: 1)** Kukhale kupempha thandizo kapena kupemphedwa kuchokere kwa munthu wamoyo ndipo kupempha izi kwa wakufa kumatchedwa 'duaau'. Munthu wakufa samamva amene angamupemphe kapena kumuitana. Allah adanena kuti: "*Mutati muwapemphe kapena kuwaitana, samamva kuitana kwanu ngakhale adakamva sadakakuyankhani*." Mwa mtundu bwanji kufunsidwa wakufa kumachita iyeyo ndi amene akusowa dua'au ya munthu wamoyo. Ameneyo ntchito zake zinadutsa chifukwa cha imfa yake kupatula zomwe malipiro ake amamufikirabe pomupempherera ndi zina zotero. Mtumiki (SAW) adati: "*Mwana wa Adam akamwalira ntchito zake zimaduka kupatula zitatu: sadaka yopitirira, kapena maphunziro amene akuthandizika nawo anthu kapena mwana wabwino amene akumamuchitira duwa*." **(Muslim)**

**2)** Adzizindikra zimene akuyankhula. **3)** Womupempherayo akhale alipo. **4)** Likhale pempholo mu zinthu zomwe zingamuthekere iye. **5)** Likhale pempholo mu zinthu za

dziko lapansi. **6)**Pempholo likhale mu chinthu chololedwa chopanda vuto mkati mwake.

**20 Kodi pemphero lodzera mwa wina lili m'magawo angati? Lili m'magawo awiri:**

**A)** Gawo loyamba ndi lomwe lili lololedwa. **Limenelo lili mitundu itatu:**

**1.** Kudziyandikitsa kwa Allah kudzera m'maina Ake ndi mbiri Zake.

**2.** Kudziyandikitsa kwa Allah kudzera mu ntchito zina zabwino, monga zomwe zili mu nkhani ya anthu atatu omwe anatsekeredwa ku phanga.

**3.** Kudziyandikitsa kwa Allah kudzera mu Duàa ya Msilamu wabwino wamoyo amene alipo amene akuganiziridwa kuti Duàa yake itha kuyankhidwa.

**B)** Gawo la chiwiri ndi lomwe lili loletsedwa, nalonso lili ndi mitundu iwiri:

**1.** Kupempha Allah kudzera mu ulemerero wa Mneneri (SAW) kapena Waliyy, monga kunena kuti Yee Mbuye wanga! Ine ndikukupemphani kudzera mwa Mneneri Wanu, kapena kudzera mu ulemerero wa Husain, mwachitsanzo, nzoona kuti ulemerero wa Mneneri (SAW) ndi waukulu pa maso pa Allah, chimodzimodzinso ulemerero wa anthu ochita zabwino, koma maswahaaba (RA) kumachita kuti iwo anali anthu akhama pochita zinthu zabwino , koma kutagwa chilala sanadziyandikitse kwa Allah kudzera mu ulemerero wa Mneneri (SAW) chikhalirecho manda ake (SAW) anali pakati pawo koma anadziyandikitsa kwa Allah kudzera mu Duàa ya amalume ake (SAW) Abbas (RA).

**2.** Kuti munthu amupemphe Mbuye wake chofuna chake momulumbirira Mneneri Wake kapena Waliyy Wake, monga kunena kuti: "Yee, Mbuye wanga! Ine ndikukupemphani chakuti kudzera mwa Waliyy Wanu wakuti. Kapena kudzera m'choonadi cha Mneneri Wanu uje," chifukwa kuchilumbirira cholengedwa pa cholengedwa nkoletsedwa, ndipo kutero pamaso pa Allah n'koletsedwa zedi, ndipo munthu alibe ufulu wolumbira motero chifukwa choti amamumvera Iye (SW).

**21 Kodi kukhulupirira tsiku lomaliza kumatanthauza chiyani?** Kumeneko ndiko kuvomereza kotsimikiza kubwera ndi kuchitika kwake, ndipo m'menemo mukulowa zokhulupirira imfa ndi zapambuyo pake, monga mayesero a m'manda, chilango cha mmanda, mtendere wa mmanda, za kuimba lipenga, kukaima anthu pamaso pa Mbuye wao, kuvundukulidwa makalata a ntchito za anthu , kuikidwa sikelo, zakuti kuli ka mlatho,chitsime, ndi Duàa ya Mtumiki (SAW), ndipo kuchokera pamenepo anthu adzapita ku Jannat kapena ku moto.

**22 Kodi zizindikiro zikuluzikulu za Kiyaamat ndi ziti?** Mneneri (SAW) anati, "*Ndithu Kiyaamat sidzabwera kufikira mudzazione zizindikiro khumi Kiyamayo isanabwere. Choncho anatchula utsi, Dajjaal, chinyama chomwe chidzatuluke pansi pa nthaka, kutuluka dzuwa komwe limalowera, kubwera kwa Issa Bin Maryam, Ya'jooj ndi Majooj, akadansana atatu: Kadansana wakuvuma, kuzambwe ndi wa pachilumba cha Arabu, ndipo chomalizira chake ndi moto womwe udzatuluke ku Yemen, udzawapirikitsira anthu kubwalo lawo losonkhanirana*" **(Muslim)**

(23) **Kodi ndi mayesero anji aakulu kwambiri omwe adzadutse pa anthu?**

Mneneri (SAW) anati "*Pakati pa kulengedwa kwa Adam (AS) kufikira tsiku la Kiyaamat pali chinthu chachikulu zedi choposa Dajjaal*" **(Muslim)**. Ndipo Dajaaliyo ndi munthu wochokera mu ana a Adam (AS) adzabwera m'nyengo yomaliza, pakati pa maso ake awiri patalembedwa zilembo izi **KAFARA** adzaziwerenga

zilembozi wokhulupirira aliyense. Ndipo iye ndi wopunduka diso lakumanja, lokhala ngati mphesa loyandama. Akadzangotulukira kumene koyamba azidzanena kuti ndi wodzakonza, kenako adzanena kuti iye ndi Mneneri, kenako adzadzitcha umulungu. Ndipo adzafika kwa anthu n'kumawaitanira anthuwo ku zofuna zake, choncho anthu adzanena kuti ndi wabodza ndi kumkanira mau ake; motero adzawachokera anthuwo nkumapita ndipo chuma chao chidzamtsatira iye nadzasanduka opanda chilichonse m'manja mwao, kenako adzafika ku anthu ndipo adzawaitanira (ku zofuna zake) ndipo adzam'vomera ndi kumkhulupirira, motero adzaulamula mtambo ndipo udzavumba mvula, ndiponso adzailamula nthaka kuti imeretse zomera ndipo idzameretsa. Adzafika kwa anthu atatenga madzi ndi moto; choncho moto wakewo udzakhala madzi ozizira, ndipo madzi akewo adzakhala moto. Ndipo zikufunika kwa wokhulupirira aliyense kuti azipempha chitetezo kwa Allah ku mayesero ake kumapeto kwa Swalaat iliyonse, ndikuti adzamuwerengere iye kumayambiriro kwa Surat KAHF ngati adzampeze, ndipo adzapewe kukumana naye powaopa mayeserowo. Mtumiki (SAW) anati: "*Amene adzamve za kufika kwa Dajjaal ayenera kuti adzamtalikire, choncho ndikulumbira Allah, ndithu munthu adzamfikira iye akuganiza kuti iye ndiwokhulupirira ndipo adzamutsatira chifukwa cha zokaikitsa zomwe zidzampangitse iye kuti amutsatire*" **(Abu Dawood)**.

Ndipo adzakhala pa dziko lapansi masiku okwanira makumi anai. Tsiku lina kutalika kwake kudzakhala ngati chaka, lina ngati mwezi umodzi ndipo lina ngati sabata, koma masiku ake onse adzakhala ngati masiku athuwa. Ndipo sadzasiya mzinda kapena dziko koma adzalowamo kupatula mzinda wa Makkat ndi Madinat, kenako adzatsika Issa (AS) ndipo adzamupha iye.

24 **Kodi Jannat ndi moto zilipo?** Eya, zilipo. Ndithu Allah adazilenga ziwirizi asadawalenge anthu, ndipo izo sizidzatha mpaka kalekale ndiponso sizidzaonongeka, ndiponso Allah analengera Jannat eni ake kudzera mu ubwino Wake, naonso moto kudzera mu chilungamo Chake, ndipo aliyense amafeweretsedwera kuchita chomwe adalengedwera.

25 **Kodi kukhulupirira chikonzero cha Allah kumatanthauza chiyani?** Kumeneko ndiko kuvomereza kotsimikiza kuti chabwino kapena vuto lililonse zimachitika ndi chigamulo cha Allah komanso chikonzero Chake (SW), ndikutinso Iye ndi wochita zimene akufuna. Mtumiki (SAW) anati: "*Ngati Allah atawalanga amene ali ku thambo Lake ndikuwalanga anthu amene ali pa dziko lapansi Lake, Iye adakamawalanga osati mowapondereza iwo ndipo ngati atawachitira chifundo, chifundo Chake chidzakhala chopambana kwambiri kwa iwo kuposa ntchito zawo. Ngati utapereka pa njira ya Allah golide ochuluka ngati phiri la Uhud, Allah sangakulandire mpaka utakhulupirira chikonzero chake ndikudziwa kuti chimene chakupeza sichinali choti chikuphonye, ndikutinso chimene chakuphonya, sichinali choti chikupeze, ndipo ngati utamwalira usakukhulupirira zimenezi unakakalowa kumoto.*" **(Ahmad, Abu Dawood).**

**Ndipo kukhulupirira chikonzero cha Allah muli zinthu zinayi:** **1)**Kukhulupirira kuti Allah amachizindikira chilichonse mwachidule komanso mwatsatanetsatane. **2)** Kukhulupirira kuti Iye anazilemba zimenezo mu Lauhul Mahfooz (ubawo wotetezedwa). Mtumiki (SAW) anati: "*Allah adalemba*

*zikonzero za zolengedwa ndi zina zotero ndipo panadutsa zaka zikwi makumi asanu (50, 000) asanalenge mitambo ndi nthaka*" (Muslim). **3)** Kukhulupirira chifuniro cha Allah chogamulidwa chomwe sichingabwezedwe ndi china chake, ndi chikonzero Chake, chomwe wafuna chimachitika, ndipo chomwe sanafune sichimachitika. **4)** Kukhulupirira kuti Allah ndiye Mlengi Wobadwitsa zinthu zonse, ndikutinso chilichonse chosakhala Iye ndi cholengedwa Chake.

**26 Kodi munthu ali ndi kuthekera komanso chifuniro choonadi?** Eya, munthu ali ndi chifuniro komanso kusankha, koma kuti zimenezi sizituluka mu chifuniro cha Allah. Allah akunena kuti:" "*Ndipo simungafune chinthu mwa inu nokha pokhapokha Allah atafuna*" (Surat 81:29). Nayenso Mtumiki (SAW) anati "*Gwirani ntchito pakuti aliyense ali wopeputsidwa pa zimene analengedwa nazo*". (Bukhuri, Muslim)

Allah anatipatsa ife nzeru , kumva ndi kupenya kuti tisiyanitse pakati pa chabwino ndi choipa. Kodi alipo wanzeru amene angabe kenako n'kumanena kuti ndithu Allah anandilembera zimenezi? Ngati atanena zimenezo, anthu sangamve dandaulo lake koma adzalangidwa ndi kuuzidwanso kuti ndithu Allah wakulemberanso chilango chimenechi.Choncho nkosaloledwa kugomezera ndi kupereka dandaulo kudzera m'chikonzero kumeneko ndikukana. Allah akunenea kuti: "*Amene akum'phatikiza Allah ndi mafano anena akadafuna Allah sitikadam'phatikiza ife ngakhale makolo athu. Ndipo sitikadaletsa chilichonse, momwemonso adatsutsa omwe adalipo patsogolo pawo*." (Surat 6: 148)

**27 Kodi ubwino ndichiyani?** Mtumiki (SAW) adafunsidwa za ubwino ndipo poyankha anati: "*Uzim'pembedza Allah ngati kuti ukumuona, pakuti iwe ngakhale kuti siukumuona ndithu Iye akukuona*" (Bukhaari, Muslim.). Limenelo ndi gawo lapamwamba mwa magawo atatu a Deen.

**28 Kodi zigawo za Tauheed zilipo zingati? Zigawo zake zilipo zitatu: 1)Tauheed ya uleri:** Kumeneko ndiye kumpatula Allah ndi ntchito Zake, monga kulenga kupereka rizq, kupereka moyo ndi zina zotero, ndipo ndithu makafiri anali kuvomera chigawo chimenechi Mneneri (SAW) asanatumizidwe. **2)** Tauheeed ya umulungu: kumeneko ndiye kum'patula Allah pomuchitira ibaadat, monga Swalaat, nazir (kulonjeza), sadaka ndi zina zotero, chifukwa chom'patula Allah pomuchitira ibaadat anatumizidwa Atumiki komanso mabuku a Allah adavumbulutsidwa. **3)** Tauheed ya maina ndi mbiri: Kumeneko ndiye kutsimikizira zomwe Allah ndi Mtumiki Wake anazitsimikizira, monga maina abwino ndi mbiri zapamwamba kukhala za Allah, mopanda kusinthanitsa kapena kuwaononga m'mene malembo alili, kapena maonekedwe, kapenanso kuyerekeza mbiri.

**29 Kodi Waliyy ndi ndani?** Ameneyo ndi munthu wokhulupirira,wochita zabwino,wa Taqwa Allah akunena kuti; "*Tamverani! Ndithu okondedwa a Allah sadzakhala ndi mantha pa tsiku la Kiyaamat, ndipo sadzadandaula; amenewo ndi amene adakhulupirira ndi kumuopa Allah*" (Surat 10 : 62-63). Nayenso Mtumiki (SAW) anati; "*Sichina, Bwenzi langa ndi Allah, komanso okhulupirira abwino.*" (Bukhaari, Muslim).

**30 Kodi n'zofunika zanji kwa ife kumbali ya Maswahaaba a Mneneri (SAW)?** Chofunika kwa ife ndi kuwakonda iwo, kuwapemphera chiyanjano cha Allah, mitima yathu kusawaganizira zoipa, komanso malirime athu kusawayankhulira

zoipa, kufalitsa ubwino wao, osanena zoipa zawo, komanso mkangano wa pakati pawo, ndipo iwo sali otetezedwa ku machimo, koma iwo anali ma Mujtahidu -ofufuza choonadi- mwa iwo anapeza choonadi, adzakhala ndi malipiro awiri, ndipo amene waphonya posapeza choonadi adzakhala ndi dipo limodzi chifukwa cha kufufuza kwake, ndipo kuphonya kwake n'kokhululukidwa. Ndipo iwo ali ndi ubwino omwe ungachotse tchimo lomwe lachitika kuchokera kwa iwo. Iwo amaposana pa ubwino. Abwino kuposa anzawo onse alipo khumi: Aboubakr, Omar, Uthmaan, Ali, Twalhat, Al-Zubeir, Abdurrahmaan Bin Aufi, Saad Bin Abii Waqqaas, Said Bin Zaid ndi Abou Ubaidah Bin Al-Jarraah. Pambuyo pa iwo ndiye Mumuhaajiruun onse (Maswahaaba osamuka kuchokera ku Makka), kenako amene adamenya nawo nkhondo ya Badr Mamuhajiruun komanso ma Answaari, otsatira apo ndiye Manswaar (Anthu a pa Madina amene adalandira anzawo osamukira mu mzindawu) otsalawo, n'kumalizirano Maswahaaba ena onse. Mtumiki (SAW) anati, "*Musawasambule Maswahaaba anga, ndikulumbira Amene moyo wanga uli m'manja Mwake, ngati mmodzi wa inu atapereka pa njira ya Allah golide ochuluka ngati phiri la Uhud sangazifike Sawabu za mlingo wamanja awiri wa chakudya wa mmodzi wa iwo kapena theka lake*".**(Bukhaari, Muslim)** . Mtumiki adanenanso kuti: "*Amene atukwane Maswahaaba anga, pa iye pakhala themberero la Allah, angero komanso anthu onse*." **(Al-tabaraniyy)**.

**31 Kodi tipyoze muyeso pomuyamikira Mtumiki (SAW) koposa muyezo umene Allah anampatsa iye?** Mosakaika kuti ndithudi Bwana wathu Muhammad (SAW) ndi wolemekezeka kwambiri mwa zolengedwa za Allah, komanso ndi wabwino wawo koposa onse, koma sizololedwa kuti tionjezere pomuyamikira monga anaonjezera Akhristu pomuyamikira Issa Ibn Maryam (AS), chifukwa iye (SAW) anatiletsa kutero ndi mau ake (SAW) onena kuti "*Musabzole malire pondiyamikira ine monga anabzolera malire Akhristu pomuyamikira mwana wa Maryam, ndithudi, ine ndine kapolo Wake (SW), choncho muzinena kuti kapolo wa Allah komanso Mtumiki Wake*". **(Bukhaari)**.

Pachiyankhulo cha Chiarabu akati: (ittwiraau) ndiko kubzoza malire poyamikira.

**32 Kodi eni Buku ndi okhulupirira?** Ayuda, Akhristu ndi otsatira zipembedzo zina ndi anthu okanira - makafiri - ngakhale ali oti akukhulupirira chipembedzo chomwe chiyambi chake n'choona, ndipo amene sanasiye chipembedzo chake pambuyo potumizidwa Mneneri Muhammad (SAW) nalandira Chisilamu, Allah akunena kuti: "*Choncho sichidzalandiridwa kwa iye. ndipo iye Tsiku Lomaliza adzakhala mmodzi mwa anthu otaika*" **(Surat 3:85)**. Ngati Msilamu sangakhulupirire zakusakhulupirira kwawo kapena kukaika za kuonongeka kwa chipembedzo chawo ndiye kuti ameneyo wasanduka kafiri chifukwa iye wanyozera chigamulo cha Allah ndi Mneneri Wake chowanena iwo kuti ndi makafiri. Allah akunena kuti; "*Ndipo amene ati asakhulupilire m'magulu a adani ndiye kuti moto ndiwo malo awo alonjezo*" **(Surat 11:17)** pakunena anthu a zipembedzo zina. Nayenso Mtumiki (SAW) ananena kuti: "*Ndikulumbira Amene moyo wanga uli m'manja Mwake. Palibe amene angandimve ine wochokera mu Ummat uno Myuda kapena Mkhristu napanda kundikhulupirira ine koma kuti akalowa ku moto*" **(Muslim)**.

**33 Kodi n'kololedwa kupondereza makafiri?** Chilungamo ndi chokakamizidwa kwa Asilamu onse, Allah (SW) wanena kuti: "*Ndithudi Allah akulamula zochita chilungamo ndi kuchitirana zabwino*." Ndipo kupondereza ndikoletsedwa m'Chusilamu chifukwa cha mawu a Allah mu Hadith Quds akuti: "*Ndithudi Ine ndadziletsa mwini Wakene kupondereza ndipo ndakuchita kuponderezako kukhala koletsedwa (haraam) pakati panu choncho musamaponderezane*." **(Muslim)**. Munthu woponderezedwa akabwezera kwa amene adamupondereza tsiku Lakiyama. Mtumiki (SAW) adati: "Kodi mumamudziwa munthu amene chamuthera chuma?" Iwo adati: "*Amene chamuthera chuma mwa ife ndi munthu amene alibe khobidi ngakhalenso katundu*." Mtumiki (SAW) adati: "*Ndithu amene chamuthera chuma mu ummat wanga ndiyemwe adzabwere tsiku la Kiyaamat ndi Swalaat, swiyaam, zakaat ndipo adzabwera atatukwana uyu, atanamizira chiwerewere uje, atadya chuma cha uyu, atakhetsa mwazi wa uje, atamenya uyu. Ndipo akampatsa uyu kuchokera mu zabwino zake, uyonso akam'patsa zabwino zake. Ngati zabwino zake zitatha asadabweze za anthu zomwe zili pa iye, akatengedwa ena mwa machimo awo n'kuponyedwa pa iye kenako nakoponyedwa ku moto*:" **(Muslim)**.
Ndiye kubwezeranaku kukachitika ngakhale pakati pa nyama.

**34 Kodi Bidah ndi chiyani?** Ibn Rajab (RA) ananena kuti tanthauzo loti Bidah ndi chinthu chomwe chaperekedwa chopanda umboni mu Shariat, tsopano chimene chili ndi umboni wochokera mu Shariat omwe ukusonyeza chinthucho, si Bidah malinga ndi zomwe anagwirizana akuluakulu odziwa malamulo a Chisilamu, ngakhale kuti chili Bidah m'chiyankhulo cha Chiarabu.

**35 Kodi mu Deen muli Bidah yabwino ndi yoipa?** M'ma Ayat a mu Quran ndi m'ma Hadith mwadza za kudzudzula mabidah mu tanthauzo lake la Shariat. Chimenechi ndi chinthu chomwe chapekedwa ndipo chilibe tsinde mu Shariat, pakuti Mtumiki (SAW) anati; "*Munthu amene wachita chinthu chosakhala mu lamulo lathu ndiye kuti chinthu chimenecho chidzakanidwa*"**(Bukhaari, Muslim)** . Ndiponso Mtumiki (SAW) anati; "*Ndithu chopeka chilichonse ndi Bidah, ndipo Bidah iliyonse ndi kusokera*" **(Abou Daaood)**.

Ponena tanthauzo la mau oti Bidah mu Shariat Imaam Maalik (RA) anati; "Amene wapeka bidah M'Chisilamu yomwe akuiona kuti ndi yabwino ndiye kuti wapeka bodza lakuti Muhammad (SAW) anachita chinyengo popereka uthenga, chifukwa Allah (SW) akunena kuti: "*Lero ndakukwaniritsirani chipembedzo chanu ndipo ndakwaniritsa pa inu chisomo changa*." **(Surat 5:3)**

Ndipo ndithu adza ma Hadith ena oyamikira Bidah mu tanthauzo lake la chiyankhulo cha Chiarabu chomwe ndi chinthu chomwe Sharia inabweretsa koma chinaiwalidwa, choncho Mneneri (SAW) analimbikitsa zowakumbutsa anthu za chinthucho, monga akunenera m'mau ake (SAW) kuti, "*Amene angayambitse M'Chisilamu Sunnat yabwino adzapeza malipiro ake komanso malipiro a amene wagwiritsa ntchito Sunnat yo pambuyo pake mopanda kupungula kalikonse m'malipiro awo*" **(Muslim).** Ndipo mu tanthauzo limeneli linadza liwu la Hadhrat Umar (RA) lonena kuti: "Taonani kukhala bwino bidah iyi", akutanthauza Swalaat ya Taraweeh, pakuti Swalaat imeneyi inali itakhazikitsidwa kale m'malamulo a

Chisilamu ndipo Mneneri (SAW) analimbikitsa za kuswali Swalaat imeneyi. Swalaat imeneyi anaiswali masiku atatu ,kenako anaisiya kuopa kuti ingasanduke kukhala lamulo lokakamizidwa, kotero Hadhrat Umar (RA) anaswali Taraweeh ndikuwasonkhanitsa anthu kuti aziswali Swalaatyo pagulu.

**36 Kodi mitundu ya Nifaaq "Uchiphamaso" ilipo ingati? Ilipo mitundu iwiri:**

**(i) Uchiphamaso wa chikhulupiriro womwe uli waukulu zedi,** komwe ndi kuonetsera chikhulupiriro ndi kubisa ukafiri, uchiphamaso umeneu umatulutsa munthu m'chipemebedzo, ndipo munthu wochita uchiphamaso umeneu ngati atamwalira akupitiriza kuchita uchiphamaso umenewo ndiye kuti wamwalira ali kafiri. Allah akunena kuti: "*Ndithu achiphamaso adzakhala pansi penipeni pa moto*" (Surat 4:145). Ndipo zina mwa mbiri zao ndi izi: Iwo amam'chita chinyengo Allah komanso amene akhulupirira, amawanyogodola anthu okhulupirira, amawathandizira makafiri powamenya Asilamu, akamagwira ntchito zawo zabwino amafuna mtendere wa dziko lapansi.

**(ii) Uchiphamaso wa m'machitidwe:** Uwu uli waung'ono. Wochita uchiphamaso umenewu sangatulutsidwe M'Chisilamu, koma kuti iye ali pa chiopsezo choti uchiphamaso umenewo utha kumufikitsa mu uchiphamaso waukulu ngati sanalape.

**Mbiri zina za mchiphamaso ndi izi:** Akati ayankhule ,amanena bodza lokhalokha, akalonjeza sakwaniritsa lonjezo, akayambana ndi munthu amangotukwana, akapangana ndi wina sakwaniritsa panganolo, akasungitsidwa kanthu amachita chinyengo. Pachifukwa chimenechi maswahaaba (RA) ankaopa uchiphamaso wamachitidwewu. Ibn Abii Mulaikat (RA) adanena kuti: "Ndidawapeza maswahaaba a Mtumiki (SAW) okwanira makumi atatu (30) aliyense wa iwo ankadziopera yekha uchiphamaso. Ibrahim Al-Taimiyy (RA) adati: 'Sindidaonetsereko liwu langa pa ntchito yanga pokhapokha ndikuopa kukhala kuti ndikunama'. Adanenanso Al-Hassan Al Baswariyy (RA) kuti: 'Palibe amene angawope (uchiphamaso) kupatula wokhulupirira weniweni komanso sangadziike pa chitetezo (choti siungam'peze uchiphamaso) kupatula mchiphamaso'. Ndipo Omar (RA) adayankhula kwa Huzaifat (RA) kuti: 'Ndikukuchonderera kudzera mu dzina la Allah, kodi adanditchulako kwa iwe Mtumiki wa Allah zoti ndili m'gulu limenelo –akutanthauza la achiphamaso-?' Iye adati: 'Ayi, ine sindiyeretsa wina aliyense pambuyo pako'.

**37 Kodi ndi tchimo lanji lomwe lili lalikulu m'machimo onse komanso ndi lowopsa kwambiri kwa Allah?** Tchimo lalikulu kwambiri kuposa machimo onse ndi la Shirk (kumuphatikiza Allah ndi cholengedwa) pakuti Allah akunena kuti " Ndithu shirk ndi kupondereza kwakukulu" (Surat 31:13), ndipo Mtumiki (SAW) atafunsidwa kuti, kodi ndi tchimo lanji lomwe lili lalikulu kwambiri? Poyankha anati: "Kuti umuikire Allah fano chikhalirecho Iye anakulenga iwe". (Bukhaari, Muslim).

**38 Kodi mitundu ya shirk ilipo ingati? Mitundu ya shirk ilipo iwiri, nayi:**

**1)** Shirk yaikulu yomwe imaam'tulutsa munthu m'Chisilamu, ndipo Allah sangamukhululukire munthu wochita shirk imeneyo chifukwa cha mau Ake (SW) onena kuti: "*Ndithudi Allah sangakhululuke atati aphatikizidwe ndi china, koma atha kukhululuka tchimo losakhala limenelo kwa amene wam'funa*." (Surat 4: 116),

**ndipo magawo ake alipo anai: a)** Shirk ya pochita Du'aa ndi popempha. **b)** Shirk ya pochita niyyat, kufuna ndi kutsimikiza kuchita, monga kuchita zabwino n'cholinga chomusangalatsa wina wosakhala Allah. **c)** Shirk ya pakumvera; monga kuwamvera ma ulama pozichita Haraam zomwe Allah wazichita Halaal, kapena kuzichita Halaal zomwe Allah wazichita Haraam. **d)** Shirk ya pachikondi, monga kumkonda wina wake monga m'mene adakam'kondera Allah.

**2) Shirk yaing'ono:** simaam'tulutsa m'Chisilamu munthu wochita Shrik imeneyo. Imeneyi ili mu zigawo ziwiri: **A)** Yowonekera chimodzimodzibe yokhudzana ndi mawu monga kulumbirira wina wosakhala Allah kapena kunena kuti: 'Zomwe wafuna Allah komanso zomwe wafuna iwe.' Komanso kuyankhula kwakuti: 'Chipanda Allah ndi uje...' kapena kukukhudzana ndi zochitikachitika monga kuvala waya ndi ulusi kuti uchotse mavuto kapena kuwapewa, komanso monga kukoleka zithumwa kuopa diso la mkhwenzule, kapena kuombeza kudzera mu mbalame, komanso maina a zinthu zina, mawu, malo ndi zina zotere. **B)** Yobisika: Iyi ndi shirk ya niyyat, zitsimikizo, khumbo monga kudzionetsera ndikufuna kutchuka.

**39 Kodi pakati pa shirk yaikulu ndi yaing'ono pali kusiyana kwanji?** Zina za kusiyana kwa pakati pa shirk ziwirizi ndizoti: shirk yaikulu imagamulidwa kwa munthu amene akuchita shirk imeneyo kuti watuluka Chisilamu dziko lino lapansi, ndikuti akakhala muyaya m'moto ku Aakhirat. Tsopano wochita shirk yaing'ono sangagamulidwe kuti watuluka Chisilamu pa dziko lino lapansi, ndipo ku Aakhirat sakakhala muyaya m'moto. Monganso shirk yaikulu imaononganso ntchito zabwino zonse pomwe shirk yaing'ono imaononga ntchito yabwino yomwe yalumikizana nayo. Ndipo ikutsala nkhani ya kusiyana kwa maganizo kuti: kodi shirik yaing'ono singakhululukidwe pokhapokha ndi toba ngati shirk yaikulu, kapena ili ngati machimo akuluakulu omwe ali pansi pa chifuniro cha Allah? Komabe ganizo lililonse mwa maganizo awiriwa pali chiopsezo chachikulu.

**40 Kodi shirk yaing'onoyi ili ndi chotchinjirizira isanachitike kapena ili ndi kulipira kwake ikachitika?** Eya, kudzitchinjiriza kwa riyaa,ndiko kusiya kudzionetsera moti adzifuna ndi ntchito yake yabwino pofuna nkhope ya Allah, tsopano kudzionetsera kwakung'ono kudzachoka podzitchinjiriza ndi Duàa. Mtumiki (SAW) anati; "*Eya, inu anthu! Ipeweni shirk iyi, pakuti imeneyi ndi yobisika kwambiri kuposa mdidi wa nyerere*. Ndipo anafunsidwa kuti: 'Kodi tingaipewe bwanji pakuti iyo ndi yobisika kwambiri kuposa mdidi wa nyerere, iwe Mtumiki wa Allah?' Poyankha anati: "*Muzinena kuti, E, Mbuye wathu ife tikupempha chitetezo Chanu kuti tisakuphatikizeni Inu ndi china chake chomwe tikuchidziwa, ndipo tikupempha chikhululuko Chanu pa chomwe sitikudziwa*" **(Ahmed)**.

Tsopano dipo la kulumbirira chosakhala Allah, ndithu Mtumiki (SAW) anati: "*Amene walumbira pomutchula laata ndi uzza awa ndi maina a mafano ayenera kuti anene mau oti Laa ilaaha illAllah kuchokera pansi pa mtima*.(Bukhaari, Muslim) .

Tsopano dipo la kuombedza ndi mbalame, ndithu Mtumiki (SAW) anati: "*Amene kwamuletsa zofuna zake kuombeza ndi mbalame, ndithu wachita Shirk*." Maswahaaba anafunsa kuti: 'Nanga kulipira kwake kuli bwanji?' Mtumiki (SAW) anati: "*Unene kuti Eya, Mbuye wanga! Palibe mtendere weniweni kupatula*

*mtendere Wanu, kapena tsoka lenileni kupatula tsoka lochokera kwa inu, ndipo palibe wopembedzedwa mwachoonadi kupatula Inu* "(Ahmad).

**41 Kodi mitundu ya ukafiri ilipo ingati? Ilipo mitundu iwiri: 1) Ukafiri waukulu womwe umam'tulutsa,** munthu m'Chisilamu; Ndipo umenewo uli m'magawo asanu. **a.** Ukafiri wa kukanira. **b.** Ukafiri wa kudzikuza pamodzi ndi kuvomera. **c.** Ukafiri wa kukaika. **d.** Ukafiri wa kunyalanyaza. **e.** Ukafiri wa uchiphamaso. **2) Ukafiri waung'ono:** komanso umatchedwa kuti kusayamika mtendere, umenewo ndi ukafiri wa kusamvera malamulo, sungam'tulutse mwini wakeyo m'Chisilamu: monga kumupha Msilamu.

**42 Kodi lamulo la nazir (kulonjeza) lili bwanji?** Mtumiki (SAW) ankakuda kulonjeza ndipo anati: "*Ndithu kulonjeza sikumabweretsa zabwino*" (Bukhaari).

Izi zili dero ngati Kulonjezako ndi kwa Allah yekha basi. Tsono kukakhala kulonjeza kosakhala kwa Allah, monga amene amalonjeza ku manda kapena Waliyy; ndiye kuti kulonjeza kumeneko n'kwa Haraam kosaloledwa, ndipo siziloledwa kukwaniritsa lonjezo lotero.

**43 Kodi ndi lamulo lanji la kupita kwa woombedza maula kapena bimbi?** Kupita kwa woombeza maula kapena kwa bimbi ndi haraam (koletsedwa). Ngati munthu atapita kwa iwo akufuna thandizo lawo koma kuti iye sadakhulupirire zodzitamandira kudziwa zobisika, ndiye kuti sidzalandiridwa kwa iye Swalaat masiku makumi anayi (40), chifukwa cha mau ake (SAW) onena kuti "*Amene wapita kwa woombeza maula namufunsa za kena kake ndiye kuti kwa iye Swalaat siidzalandiridwa masiku makumi anayi*" (Muslim). Ndipo ngati atapita kwa iwo nawakhulupirira zodzitamandira kwawo zoti amadziwa zobisika,ndiye kuti wakanira Deen ya Muhammad (SAW) chifukwa cha mau ake (SAW) onena kuti: "*Amene wapita kwa woombeza maula kapena kwa bimbi namukhulupirira pa zimene akunena ndiye kuti ndithu wakanira chimene chinavumbulutsidwa kwa Muhammad (SAW) (Quràn).*" (Abu Dawood).

**44 Kodi kukhala ndi maganizo oti mvula imapezeka chifukwa cha nyenyezi kungakhale shirk yaikulu kapena yaing'ono nthawi yanji?** Amene wakhulupirira kuti nyenyezi ili ndi mphamvu (yodzetsa mvula) popanda chifuniro cha Allah, naika mgwirizano wa mvula ndi nyenyezi podzetsa mvula, ndiye kuti imeneyi ndi shirk yaikulu. Tsopano amene wakhulupirira kuti nyenyezi ili ndi mphamvu yodzetsa mvula n'chifuniro cha Allah ndikutinso Allah anaichita nyenyeziyo kukhala chifukwa chotsikira mvula, ndikutinso Allah (SW) anaika chizolowezi cha kupezeka kwa mvula ikaoneka nyenyezi imeneyo, ndiye kuti chikhulupiriro chimenechi ndi cha Haraam komanso shirk yaing'ono, chifukwa munthuyo azichita zimenezo kukhala chifukwa chotsikira mvula mopanda umboni wochokera mu shariat, kapena mu nzeru zangwiro.Tsopano kulondolera ndi nyenyezizo, nyengo za pa chaka, ndi nthawi yofufuzira kutsika kwa mvula, zimenezo ndi zololedwa.

**45 Ndi chiyani chofunika kwa atsogoleri a Asilamu?** N'zofunika kuti anthuwo kuwamvera pa mtendere ndi pa mavuto, ndipo sizikuloledwa kuwaukira iwo atsogoleriwa ngakhale ataponderezа, tisawapempherere zachabe, tisasiye kuwamvera, tiwachitire Duàa yoti akhale abwino, amoyo wangwiro ndinso achiongoko,olungama.

Tiziona kuti kuwamvera iwo ndiko kumumvera Allah ngati iwo sakulamulira zolakwira Allah. Ngati iwo alamulira zolakwira Allah ndi za haraam n'koletsedwa kuwamvera mu zimenezo, ndipo zidzakhala waajib kuwamvera iwo ku zinthu zabwino zosakhala zoipa. Mtumiki (SAW) anati: "Umve ndi kumvera mtsogoleri, ngakhale utamenyedwa msana wako ndikutengedwa chuma chako, umve komanso umvere" (Muslim)

**46 Kodi zikuloledwa kufunsa cholinga cha Allah mu zolamula ndi zoletsa?** Inde, koma padzafunika kuti kukhulupirira kapena kugwira ntchito zisadalire pa kudziwa cholinga ndi kuchikhutira, pakuti kudziwa kumakhala kuonjezera kukhazikika kwa munthu wokhulupirira pa choonadi; koma kuvomereza kopanda malire ndi kusafunsa ndi umboni wosonyeza kukwanira kudzionetsera ukapolo ndi kukhulupirira mwa Allah ndi luntha Lake lokwanira monga momwe ankachitira Maswahaaba (RA).

**47 Kodi mau a Allah onena kuti "*Chabwino chimene chakupeza ndiye kuti chachokera kwa Allah, ndipo choipa chomwe chakupeza ndiye kuti chachokera kwa iwe mwini*" (surat 4 : 79) akutanthauza chiyani?** Tanthauzo loti chabwino apapa akunena mtendere ndipo choipa akunena tsoka. Koma zonsezo zili m'chikonzero cha Allah, choncho chabwino achipereka kwa Allah chfukwa choti, Iye ndi amene wapereka mtendere, tsopano choipa, ndithu anachilenga ndi cholinga, ndipo icho molingana ndi cholingacho chikuchokera mu ubwino Wake, koma kuti zochita Zake zonse ndi zabwino. Mtumiki (SAW) anati: "*Ndipo zabwino zonse zili m'manja Mwako, ndipo vuto silili kwa Iwe*." (Muslim) Choncho zochita za akapolo a Allah ndizolengedwa ndi Allah, zomwenso ndi ntchito za akapolo mu nthawi yomweyo, Tsono yemwe akupereka pa njira ya Allah akumuopa Mbuye wake. *Ndikumavomereza zinthu zabwino, timaamufewetsera njira yopititsa ku zabwino*." (Surat 92:5 - 7)

**48 Kodi zikuloledwa kuti ndinene kuti uje ndi shaheed?** Kugamula za wina wake kuti ndi Shaheed ndi chimodzimodzi kugamula kuti iye akalowa ku Jannat, ndipo Mazhab Ahlus - Sunnat ndiwoti tisanene mosankha wina wake mwa Asilamu kuti iye ndi wa ku Jannat kapena ku moto kupatula yemwe Mneneri (SAW) anamunena kuti ndi wa ku Jannat kapena ndi wa ku moto, chifukwa zoona zake zenizeni n'zobisika, ndipo sitikudziwa chomwe munthu anali nacho pomwe amamwalira, ndipo zochitika zimatengedwa kumapeto kwake ndipo kuzindikira Niyyat kuli m'manja mwa Allah, koma tikhale ndi chiyembekezo choti wochita zabwino akapeza Sawabu, ndipo munthu wochita zoipa timuopere chilango.

**49 Kodi zikuloledwa kugamula kwa Msilamu wina wake kuti ndi kafiri?** Sizikuloledwa kuti tigamule kwa Msilamu wina wake kuti ndi kafiri, wa shirk kapena wa uchiphamaso, ngati sichinaonekere china chake kuchokera kwa iye chosonyeza zimenezo, ndipo tichotse zolepheretsa munthuyo kukhala Msilamu, ndiponso timusiyire Allah zinsisi zake.

**50 Kodi zikuloledwa kuchita Twawaaf chinthu chosakhala Ka'bah?** Pa dziko lapansi sapezeka malo wololedwa kuwachita Twawaaf kupatula Ka'bah yolemekezeka, ndipo sizikuloledwa kuwafanizira malo ena alionse ndi Ka'bah ngakhale atakhala wolemekezeka chotani, amene angachichite Twawaaf chosakhala Ka'bah mochilemekeza ndiye kuti ndithu wamunyoza Allah.

# NTCHITO ZA MITIMA

Allah adalenga mtima ndipo adauchita kukhala mfumu ndipo ziwalo zake ngati asirilkali ake. Ngati mfumu ikhale yabwino ndiye kuti asirikali akewonso akhalanso abwino. Mtumiki (SAW) adati: "*Ndithu mu thupi la munthu muli mnofu ukakhala bwino umenewo ndiye kuti thupi lonse likhala bwino. Pamene mnofu umenewu ukaipa thupi lonse limaipa, zindikirani, mnofu umenewu ndi mtima*." (Bukhar, Muslim) Mtima, awo ndi malo a Imaan (chikhulupiriro) ndi Al-Taqwah (kuopa Allah), kapena ukafir, uchiphamaso kapenanso shirk. Mtumiki (SAW) adati: "*Kuopa Allah kuli apa". Uku akulozera pa chifuwa pake katatu*." (Muslim).

**Tsono Imaan (Chikhulupiriro):** ndicho chitsimikizo, liwu ndi ntchito. Chitsimikizo cha mtima, liwu la lirime ndi ntchito za mtima komanso ziwalo. Mtima umakhulupirira komanso kuvomereza ndi pameneno pamabweretsa liwu la chikhulupiriro lonena shahaadah pa lirime kenako mtima umagwira ntchito zake monga chikondi, mantha,chiyembekezo. Komanso lirime limatekeseka potchula Allah ndi kuwerenga Quran. Ndipo ziwalo zimatekeseka polambira Allah (sujuudu), kuwerama (rukuu) ndi kugwira ntchito zabwino zomwe zingayandikitse kwa Allah. Thupi limatsatira mtima, nkosatheka kukhazikika chinthu mu mtima pokhapokha zimaonekera zabwino kapena zotsatira zake pa thupi kapena m'njira ina ili yonse.

**Tanthauzo la ntchito za mtima: izi ndi ntchito zimene malo ake amakhala mu mtima ndipo zimagwirizana nawo. Yaikulu kwambiri mu ntchitozi ndikukhulupirira mwa Allah yomwe imakhala mu mtima. Zinanso mwa izo ndikuvomereza zomwe zimapezeka mu mtima mwa kapolo pa za Mbuye wake monga chikondi, mantha, chiyembekezo,kudzichepetsa ndi zina zotero.**

Ntchito ili yonse mu ntchito za mtima mtsutso wake ndi nthenda mu matenda a mtima. Kudziyeretsa mtsutso wake ndi kudzionetsera. Chitsimikizo mtsutso wake ndi chikaiko. Chikondi mtsutso wake ndi kuipidwa ndi zina zotero. Ife tikaiwala za kukonza mitima yathu, ndiye kuti ayanga machimo pa mitimayo nkutiononga. Mtumiki (SAW) adati: "*Ndithudi kapolo akachita tchimo, pamaikidwa pa mtima wake dontho. Iye akalitalikira tchimolo napempha chikhululuko nkulapa, dontholo limachotsedwa. Iye akabwerera ku tchimo lija, dontholo limaonjezereka mpaka limakula mwa iye, limenelo ndi dzimbiri limene Allah adalitchula*. "*Ayi koma kuti mitima yawo yachita dzimbiri chifukwa cha ntchito zimene ankachita*". Tirmidhi.

Ndiponso Mtumiki (SAW) adati: "*Mayeserero amaonetsedwa kwa mitima monga ikhalira mphasa, wale limodzilimodzi. Ndiye mtima ulionse umene ukhutitsidwe ndi mayeserero umaikidwa dontho lakuda. Pamene mtima ulionse udabwe nkukana mayesererowa umaikidwa dontho loyera kufikira kuti imasanduka mitima iwiri ija, woyera uja kukhala woyeretsetsa ngati madzi woyera ndiye siuvututsidwa ndi mayeserero alionse nthawi zonse m'mene mitambo ndi nthaka zikhalire. Unzake uja nkukhala wakuda kwambiri ngati nsanjiro yotembenuzidwa siudziwa chabwino kapena kunyansidwa ndi choipa kupatula zokhazo zimene udakhutitsidwa nazo za chilakolako chake*." (Muslim).

**Kudziwa ibaadat ya mitima** ndikokakamizidwa kwambiri komanso nkofunika kwa kapolo kuposa kudziwa ntchito za ziwalo chifukwa limenelo ndilo phata pamene ntchito ya ziwalo ndi nthambi za m'menemo zokwaniritsa komanso

chipatso chake. Mtumiki (SAW) adati: “*Ndithu Allah sayang’ana nkhope zanu kapena chuma chanu koma amayang’ana mitima yanu ndi ntchito zanu*.” (Muslim).

Mtima ndi malo a kuzindikira, kuganiza ndi kulingalira.Ichi n’chifukwa chake kuposana kumene kungakhale pakati pa anthu kwa Allah kuli malinga ndi zomwe zakhazikika mu mtima monga chikhulupiriro, chitsimikizo, chiyero ndi zina zotero. Adanena Al Hassan Al-Baswariyy (RA) kuti: “Ndikulumbira Allah, sikuti Aboubakr (RA) adaposa azinzake ndi Swalaat kapena swaum ayi koma anaposa ndi chikhulupiriro chomwe chidakhazikika mu mtima mwake.”

**Ndipo ntchito za mitima zimaposa ntchito za ziwalo mu njira izi**: **1)** Ndithudi kuonongeka kwa ibaadat ya mtima nkutheka kugumula ibaadat ya ziwalo monga kudzionetsera kukakhala pa ntchito. **2)** Ntchito za mtima ilo ndi thanthwe- malo a maziko- ndipo zomwe zingachitike monga liwu kapena kutekeseka kopanda chitsimikizo cha mtima, palibepo kulangidwa nazo. **3)** Ntchito za mitimazi ndithudi ndi njira zopezera masitepe apamwamba a ku Jannat monga kusalabadira za m’dziko. **4)** Ndikutinso zimenezo ndi zovuta komanso zouma kuzichita kuposa ntchito ya ziwalo. Akunena Ibn Al –Munkar (RA) kuti: “Ndazunzika nawo mtima wanga kwa zaka makumi anai (40) kufikira mpaka udaongoka nkukhala wangwiro kwa ine.” **5)** Ntchito za mitimazi ndithudi nzokongola m’zotsatira zake monga kukonda chifukwa cha Allah. **6)** Komanso zimakhala ndi malipiro aakulu. Adanena Abou Al Dardaai (RA) kuti: “Kulingalira kwa ola limodzi kumaposa kuima kupemphera usiku onse.” **7)** Ndithudi izi ndizomwe zimapatsa mphamvu ziwalo kuti zigwire ntchito. **8)** Ndithudi zimenezinso zimakuza malipiro a ibaadat ya ziwalo kapena kuchepetsa mwina ngati sikuononga kumene monga kudzichepetsa pa Swalaat. **9)** Ndikutinso ibaadat ya mitima imatheka kutenga malo a ibaadat ya ziwalo monga chitsimikizo (niyyat) chopereka sadaka, chuma palibe. **10)** Ndikutinso ibaadat ya mitimayi malipiro ake alibe malire monga kupirira. **11)** Ndithudi malipiro ake amapitirira ngakhale ziwalo zitaima kapena kulephera kugwira ntchito. **12)** Komanso ibaadat imeneyi imakhalapo kusadapezeke ntchito za ziwalo koma kukhalira limodzi zikamachitika.

**Ndipo ziwalo sizadagwire ntchito mtima umadutsa mu zinthu izi: 1) Lingaliro:** ili ndi ganizo likangofika kumene mu mtima. **2) Ganizo:** ili ndi lingaliro limene lakhazikika mu mtima. **3) Nkhani za mtima:** uku ndiko kukaika kodi achitedi chinthucho kapena asiye. **4) Kujjirika:** uku ndiko kuona mbali imene ikutenga malo kwa iyeyo pofuna kuchita chinthucho. **5) Kutsimikiza:** izi ndi mphamvu zotsimikiza ndikuikira mtima kuchita basi.

zitatu zoyambirira zija zilibe malipiro pa chabwino komanso palibe tchimo pa choipa. Tsono kujjirika, kukakhala pa chabwino amalemberedwa chabwino chimodzi ndipo kukakhala pa choipa salemberedwa choipa. Kenako kujjirika kumabala chitsimikizo kukhala popanga chabwino amalipidwa ndi chabwino ndipo kukakhala popanga choipa, ndiye kuti wachita tchimo angakhale sadachichite. Zili dero chifukwa kufunitsitsa kukakhala limodzi ndi kuthekera kumachititsa kupezeka kwa chinthu cholinganizidwacho. Allah Tabaarakaat Wataalaa akunena kuti: “*Ndithudi anthu amene akukonda kuti zoipa zifalikire mwa anthu okhulupirira, ali*

*nacho chilango chopweteka.*" Ndipo Mtumiki (SAW) adati: "*Akakumana Asilamu awiri ndi malupanga awo (wina nkupha mnzake) ndiye kuti wakupha ndi wophedwayo onsewo akalowa ku moto." Ndidati: 'Eh iwe Mtumiki (SAW) ! Zikumvekadi kwa uyu wakuphayu nanga vuto lili pati kwa wophedwayo ?' Mtumiki (SAW) adati: 'Ndithudi iyeyo amachitira khama kuti aphe mnzakeyo (zangomulaka)*. (Bukhaari).

**Ngati wina atasiya tchimo pambuyo potsimikiza kulichita ndiye kuti munthuyo amakhala mu zigawo zinai izi:**

**1.** Walisiya chifukwa choopa Allah: uyu amalipidwa zabwino.

**2.** Walisiya chifukwa choopa anthu: uyu wachita tchimo chifukwa kusiya tchimo ndi ibaadat ndiye nkoyenera kuzikhala chifukwa cha Allah.

**3.** Walisiya chifukwa chakulephera iye sadachite njira zimene zingam'fikitse ku tchimolo: uyu amapezanso machimo chifukwa cha chitsimikizo chenichenicho.

**4.** Walisiya chifukwa chakulephera atachita njira zonse zimene zingamufikitse ku tchimolo koma cholinga chake sichidatheke: Uyu alembedwa tchimo la munthu amene walichitadi mokwanira chifukwa khumbo la chitsimikizo limene labwera nalo nkutheka kukhala ntchito yom'tengera mwini wakeyo mayendedwe a wochita weniweniyo monga m'mene zatsogola mu hadith ija. Nthawi zonse ntchito zikalumikizana ndi kujjijirika, ndiye kuti ndithudi alangidwa nayo kaya kuichitako kwachedwa kapena kwafulumira. Munthu amene wachita chinthu choletsedwa kenako natsimikiza zochichitanso nthawi ili yonse imene angathe ndiye kuti ndiwaliuma pa tchimo ndipo alangidwa ndi chitsimikizo chakechi angakhale sanabwererenso ku ntchito yakeyi.

# ZINA MWA NTCHITO ZA MITIMA

**NIYYAT (CHITSIMIKIZO):** Ili ndilo tanthauzo la chikhumbokhumbo ndi chitsimikizo: Ntchito ya munthu siivomerezeka kapena kulandiridwa pokhapokha patakhala niyyat. Mtumiki (SAW) adati: "***Ndithudi ntchito zonse amalipidwa nazo malinga ndi niyaat – zolinga zake – ndipo munthu aliyense akapeza chimene analinga***." (Bukhar, Muslim). Ndipo Ibn Al-Mubaarakaath (RA) adanena kuti: 'Mwina ntchito yochepa imakulitsidwa ndi niyyat (cholinga) mwinanso ntchito yaikulu ingachepetsedwe ndi niyyat.' Ndiponso Al-Fadheel (RA) adati: 'Ndithudi chimene akufuna Allah mwa iwe ndi niyyat yako ndi chifuniro chakocho. Ikakhala ntchitoyo yomuchitira Allah imatchedwa chiyero, uko ndiko kukhala ntchitoyo yoyeretsedwa yomuchitira Allah ndipo wina aliyense wosakhala Iye alibemo gawo m'menemo. Ikakhala ntchitoyo siyom'chitira Allah imatchedwa kudzionetsera kapena uchiphamaso ndi zina zotero.

**PHINDU:** Anthu onse ndi owonongeka kupatula ozindikira; komanso onse ozindikira ndi owonongeka kupatula mwa iwo ogwira ntchito (ndi kuzindikira kuja). Ogwira ntchito onse ndi owonongeka kupatula odziyeretsa. Ndiye ntchito yoyamba pa kapolo amene akufuna kumvera Allah ndiye kuphunzira niyyat kenako ndikuikonza ndi ntchito pambuyo pomvetsa kuona mtima ndi kudziyeretsa. Ndipo ntchito yopanda niyyat kumeneko ndi kungodzitopetsa, pamene niyyat yopanda chiyero ndi kudzionetsera ndipo chiyero chopanda kutsimikizira ndi chikhulupiriro ndi fumbi lakhoboo.

**Ndipo ntchito zili mitundu itatu:**

**1) Za Haraam -Machimo**: niyyat yabwino pa tchimo sikungalisandutse kukhala kumvera Allah kudzera mu chitsimikizo chabwino kungoti chitsimikizo choipa chikaonjezereka pa tchimo, tchimo lake limawonjezereka.

**2) Mubaahaat- Zovomerezeka:** Palibe pa chinthu chili chonse cha Mubaah pokhapokha mumakhalamo niyyat ndipo n'kutheka munthu atafuna, kuzisandutsa zinthu zodziyandikitsira kwa Allah.

**3) Twa aat –Zomumvera malamulo a Allah**: Izi ndiye zimaamangana ndi niyyat pa tsinde lakuvomerezeka kwake ndikuwonjezeredwa kwa malipiro ake.[1] Ngati atatsimikiza kudzionetsera chimakhala tchimo komanso shirk yaing'ono nkutheka kukhalanso pa mulingo wa shirk yaikulu yomwe ili mu njira zitatu:

**A)** Kukhala chikhumbokhumbo chochitira ibaadat ndi kudzionetsera kwa anthu kuyambira pa phata ndiye kuti imeneyo ndi shirk ndipo ibaadat imeneyo ndi yowonongeka - yosavomerezedwa.

**B)** Kukhala ntchitoyo ndi yom'chitiradi Allah kenako n'kulowamo kudzionetsera. Ndiye ikakhala ibaadat yake mapeto ake samamangidwa ndikudalira chiyambi chake monga sadaka, ndiye kuti koyambirirako kuli bwino – kovomerezeka- ndipo komalizira kwakeko nkolakwika – kosavomerezeka. Ngati ntchitoyo amamangidwa mapeto ake pa chiyambi chake monga Swalaat ndiye magawo awiri: **1-** Alimbane ndi kukukankha kudziotserako, ndithudi izo zikhala zopanda vuto pa ntchitoyo. **2-** Akakhazikitsa mtima pakudzionetserapo ndithudi ibaadat yonseyo imaonongeka.

**C)** Kupezeka kodzionetsera pambuyo pakugwira ntchitoyi: Awa ndi manong'onong'o

---

[1] **Mtumiki (SAW) adati:** "*Amene angajijirike kuchita chabwino ndipo sadachichite, Allah amamulembera chabwino chokwanira. Ngati iye atajijirika kuchichita nkuchichitadi, Allah amamulembera nacho kwa Iye zabwino khumi mpaka zowonjezera zikwi makunu asanu ndi awiri* (700) *kumapitiriranso apo pazowonjezera zambirimbiri. Amene wajijirika kuchita cholakwa koma iye sadachichite (wadziletsa kuopa Allah), Allah amamulembera nacho kwa Iye chabwino chimodzi chokwanira. Ngati atajijirika ndi tchimolo nalichitadi, Allah amamulembera kwa Iye cholakwa chimodzi*." **Bukhar, Muslim.** **Ndipo Mtumiki (SAW) adati:** "*Fanizo la ummat uwu lili ngati fanizo la anthu anayi. (Woyamba) ndi munhtu amene Allah adampatsa chuma ndi maphunziro, iye nkumagwiritsira ntchito maphunziro akewo pa chuma chake nkumachiperekera mu njira yoyenerera yake. Wina (wachiwiri) ndi munthu amene Allah wamupatsa maphunziro koma sadampatse chuma ndipo iye nkumati 'nkadakhala ndi chuma chonga ichi (cha uje amene akuchiperekera pa njira ya Allah), bwenzi ndikuchita m'mene ujeyu akuchitira'. Mtumiki (SAW) adati: "Awiriwa pa malipiro abwino ali chimodzimodzi. Ndipo wina (wachitatu) ndi munthu amene Allah wamupatsa chuma koma sadampatse maphunziro iye nkumachisakaza chumacho nkumachiononongera m'malo osayenerera. Komanso munthu wina (wachinayi) ndi amene Allah sadam'patse maphunziro ngakhalenso chuma koma iye n'kumati 'N'kadakhala nacho chuma chofanana ndi cha uje (wosakazira uja pa zinthu zimene Allah amadana nazo), bwenzi ndikuchita monga akuchitira ujeyu' .Mtumiki adati: 'Ndiye kuti awiriwanso pa tchimo ndi ofanana*.' **Tirmidhi.** Kuyankhula kwa wachiwiriyu komanso wachinayiyo mu hadith imeneyi, apatsidwa izi chifukwa ndizotheka chomwe ndi niyyat pamodzi ndi kulakalaka , kusirira ndipo zawonekera zimenezi m'kuyankhula kwawo koti: " N'kadakhala nazo zonga izi bwezni ndikuchita umo akuchitira ujeyu." Ndiye aliyense wa awiriwo akaphatikizidwa ndi mnzake uja pa malipiro komanso pa tchimo.
**Ibn Rajab (RA) adati:** 'Kuyankhula kwake mu hadithyi koti: 'Awiriwo pamalipiro ndi ofanana kukusonyeza kufanana kwa awiriwo pa phata la ntchityo osati kuwonjezereka. Tsono kuonjezereka kukukhudzana ndi munthu amene waigwiradi ntchitoyo osati amene amangochita niyyatyu ndipo sanaigwire chifukwa awiriwa adakafanana mu njira zonse bwenzi akumulembera amene anajijirika kuchita chabwino ndipo sadachichite- zabwino khumi zomwe zikusemphana ndi malamulo onse.

a Satana alibe vuto lili lonse pa ntchitoyi kapena pa amene waigwirayo. Palinso mitu ingapo yobisika yofotokoza za kudzionetsera pafunika kuidziwa ndi kuipewa.

**Tsono chikakhala cholinga chake kugwira ntchitoyo cha za dziko lapansi kuti azipeze, ndithudi malipiro kapena tchimo lake limakhala pa mulingo wa niyyat yake ndipo ali m'magawo atatu: 1)** Kukhala chikhumbokhumbo chchitira ntchitoyo chili pa za dziko basi, mwachitsanzo munthu amene akupempheretsa anthu pa Swalaat kuti adzipeza chuma, uyu ngolakwa ndipo ali ndi machimo. Mtumiki (SAW) adati: "*Munthu amene waphunzira maphunziro amene amafunikira nawo kupeza nkhope ya Allah, koma iye sakuwaphunzirira chifukwa china kupatula kuti apeze zopeza za pa dziko, sakapeza fungo la Jannat tsiku la Kiyaamat*." **Abou Daood.**

**2)** Kugwira ntchito pofuna nkhope ya Allah komanso panthawi yomweyo kufuna za dziko lapansi, ndithu woteroyo ndi wopunguka chikhulupiriro komanso chiyero monga munthu amene akukachita Hajj chifukwa choti akachite malonda ndiye kuji Hajjyo malipiro akakhala pa mulingo wa kudziyeretsa kwake.

**3)** Kugwirira ntchitoyo chifukwa cha Allah yekha basi koma amatenga malipiro woti adzithandizika nawo pogwira ntchitoyo, ndiye kuti malipiro a ntchito yakeyo kwa Allah ndiwokwanira moti zimene amalandirazo sizipungula kalikonse. Mtumiki (SAW) adati: "*Ndithu chinthu choyenerera kutengerapo malipiro, ndi Bukhu la Allah*." **Bukhar.**

**Zindikira kuti odziyeretsa ogwira ntchito ali m'masitepe awa: a) Yapansi:** imeneyi ndiyo yoti akugwira ntchito yomvera Allah akuyembekezera malipiro (sawabu) kapena kuopa chilango. **b)Yapakatikati:** Kugwira ntchito yomvera Allah chifukwa chakuyamika Allah ndikuvomera malamulo Ake. **c) Yapamwamba:** Kugwira ntchito yomvera Allah mwachikondi,kumukuza, kumulemekeza ndi kumuopa Allah, iyi ndiyo sitepe ya ma swiddiiqeena[1]-anthu owona mtima.

**◗ TAUBAT (KULAPA):** Ndikokakamizidwa nthawi zonse ndipo kugwa m'machimo ndi chikhalidwe cha munthu. Mtumiki (SAW) adati: "*Mwana wa Adam aliyense ngolakwitsalakwitsa ndipo abwino a olakwitsalakwitsa ndi awo amene amalapa*." **Tirmidh.** Ndipo Mtumiki (SAW) adati: "*Mukadamapanda kumalakwa, bwenzi Allah atakuchotsani ndikubweretsa anthu amene azilakwa n'kumam'pempha Allah chikhululuko, n'kumawakhululukira*." **(Muslim).**

Choncho kuchedwetsa kulapa ndikupitiriza pa cholakwika ndi tchimo (sambi). Satana akufuna kumpeza munthu kuchokera mu zikweza (mikwingwirima) isanu ndi iwiri (7) akalephera wina amapita ku umnzake.

**1)** Mkwingirima wa shirk ndi ukafiri. **2)** Akapanda kutheka apo ndiye amakukokera ku zinthu zopeka m'chikhulupiriro (bid'ah) ndikusiya kutsatira Mneneri (SAW) ndi

---

[1] Allah (SW) wati: "*Ndipo ndafulumirira kwa Iwe kuti usangalale*." Ndiye kuti Musa (AS) adachitira khama pofulumizitsira zokakumana ndi Allah kuti Allah asangalale naye. Sikunali kuvomera kokha lamulo Lake ayi. Chofanana nacho ichi ndiko kuchitira zabwino makolo:sitepe yapansi ndiko kuwachitira zabwino kuopa chilango chonyoza makolo ndi kufuna malipiro abwino. Sitepe yapakatikati ndiyo kuti ukuwachitira zabwino chifukwa chovomera malamulo a Allah ndikubwezera zabwino zawo pa iwe pokulera uli wamng'ono, ndikuti awiriwo anali njira yakupezeka kwako pano pa dziko. Sitepe yapamwamba: ndiyo kuti iwe kuwachitira zabwino pofuna kukuza lamulo la Allah lochitira makolo zabwino ndikukonda komanso kulemekeza Allah.

Maswahaba ake. **3)** Akapanda kutha izo ndiye amamukokera munthuyo kuchita machimo aakuluakulu. **4)** Akalephera apo , tsono amamuchititsa kuchita machimo aang'onoang'ono. **5)** Ngati atakanika pamenepa,ndiyeno amamuchulukitsira zinthu zovomerezeka (zamubaah) kuti azizichita. **6)** Akalephera apo ndiyeno amam'pangitsa munthuyo kuti adzichulukitsa kuchita zinthu zomvera Allah osati zomwe zili zabwino kuposa izozo kapena zazikulu malipiro ayi. **7)** Ngatinso apo akulephera ndiyeno amamuikira asatana a munthu ndi ziwanda (kuti adzimutsatatsata mpaka amupomphonetse).

**Tsono machimo ali mu zigawo izi: 1) Aakuluakulu:** Amenewa ndi machimo amene muli chilango pano pa dziko kapena chiopsezo cha chilango pa tsiku lomaliza kapenanso temberero mwinanso mkwiyo wa Allah kapena kukanidwa kwa chikhulupiriro. **2) Aang'onoang'ono:** Awa ndi ocheperako pa mulingo.

**Pali zifukwa zimene zimasandutsa machimo aang'onoang'ono kukhala aakuluakulu. Zofunikira zake ndi:** Kukakamira kuwachita ang'onoang'onowo, kapena kuwabwerezabwereza, kapena kuwapeputsa mwinanso kunyadira kuti wakhoza kuwachita ndi kuwonetsera poyera powachita.

Tsono taubat (kulapa) nkovomerezeka pa machimo onse ndipo kukadalipo kufikira kutuluka kwa dzuwa kuchokera kuzambwe kupita kuvuma kapena kufika kwa mtima wa munthu pachidali (pakholingo) nthawi ya imfa. Tsono malipiro a munthu wolapa ngati mu kulapa Kwake kuli kowona mtima, ndiye kuti amakhala kusandutsidwa machimo aja kukhala zabwino angakhale atafika kumwamba kwa thambo kuchuluka kwake.

**Taubat kuti ilandiridwe ili ndi malamulo ake awa: 1)** Kusiiratu tchimo. **2)** Kudzinena pa zimene zidapita. **3)** Chitsimikizo cholimba choti sadzabwerezanso kulichita tchimolo mtsogolo. Ndipo likakhala tchimo lokhudzana ndi katundu wa anthu ndiye nkoyenera kubweza katunduyo amene udatenga kuchokera kwa iwo mopondereza kwa eni ake[1].

**Ndipo anthu akalapa ali mmagulu anayi:**

**1.** Wolapa amene ali wangwiro pakulapapo kufikira mathero amoyo wake ndipo samadziyankhulitsa (mu mtima mwake) zobwerera ku tchimo lakelo kupatula kuthyerezuka komwe munthu sangasiyane nako. Uwu ndiwo ungwiro pa kulapa. Mwini wakulapa kumeneku ndiye wotsogola pa zabwino. Ndiye kulapa kumeneku kumatchedwa Al –Nasuuha- kulapa kwenikweni. Uwu ndiwo mzimu wodekha.

---

[1] kwanenedwa kuti ndithudi Mtumiki (SAW) adati: "*Akaundula olembamo ntchito za anthu kwa Allah alipo atatu. Kaundula yomwe Allah amangolisiya wosaikiramo mtima kanthu kalikonse, (wachiwiri) kaundula amene Allah sasiyamo kanthu kena kali konse m'menemo, ndipo wachitatu ndi amene Allah sakhululuka. Tsono kaundula amene Allah sakhululuka ndi shirk. Allah wati:* "*Ndithudi amene aphatikize Allah ndi china chake ndithudi Allah wachita haraam kwa iye Jannat (sakainunkha) ndipo malo ake akakhala ku moto*." *Tsono kaundula amene Allah samamusamala kanthu kalikonse ndiye kupondereza kwa kapolo podzipondereza yekha pa zinthu zomwe zili pakati pake ndi Mbuye wake. Ndithu Allah akafuna amam'khululukira zimenezo ndi kuzisiirira. Tsono kaundula amene Allah sasiyamo kanthu kalikonse ndiye kuponderezana kwa akapolo wina ndi mnzake. Apa, mosakaika, pafunika kubwezerana basi*." **(Ahmad koma hadithyi ndiyofookerapo)**

**2.** Wolapa amene ali ngwiro pa ntchito zikuluzikulu zomvera Allah kupatula kuti iyeyo salekana- satayana- ndi machimo amene amam'peza apa ndi apo osati mwadala. Iyeyo amayesedwa ndi machimowo popanda kuwapitira motsimikiza powachita. Nthawi zonse akachita kanthu mwa izi amadzidzudzula yekha, kudzinena ndi kutsimikiza kutalikira njira zake. Uwu ndwo mzimu wodzidzudzula.
**3.** Kulapa nakhala ngwiro kanthawi, kenako zilakolako zake nkumugonjetsa pa machimo ena nawachita kupatula kuti ngakhale zili dero, iye ndi wozolowera kugwira ntchito zomvera Allah. Ndipo iye wasiya machimo ambiri angakhale ali nako kuthekera pa machimowo komanso chilakolako chake. Kungoti ndithudi iyeyo chilakolako chimodzi kapena ziwiri chimaamugonjetsa ndipo chikatha nadzinena koma akuwulonjeza mtima wake zolapa, kusiya tchimo lija. Uwu ndi mzimu wofunsidwa. Mapeto ake ndi oopsa kumbali yochedwetsa ndi kuchita bobobo pakuti mwina akhoza kufa asadalape, potitu ntchito za munthu zimawerengedwa ndi zimene watsirizira.
**4.** Amene walapa ndikulungama kwakanthawi kenako nabwerera ku machimo ndi mutu onse popanda kudziuza za kulapa komanso mosadandaula pa zochita zakezo. Uwu ndi mzimu wa dzimbiri ndipo ameneyu akuopedwera mapeto achabe.

◗ **KUONA MTIMA (kunena zoona):** Kunena zoona kapena kuona mtima: ili ndi tsinde la ntchito zonse za mu mtima. Liwu loti kunena zoona limagwiritsidwa ntchito pa matanthauzo asanu ndi limodzi: **1)** Kunena zoona poyankhula. **2)** Kuona mtima pa chikhumbokhumbo ndi chitsimikizo (chiyero). **3)** Kuona mtima pa chitsimikizo. **4)** Kuona mtima pokwaniritsa ndi chitsimikizo. **5)** Kuona mtima pogwiritsa ntchito moti zoonekera zake zifanane ndi zobisika zake monga kudzichepetsa pa Swalaat. **6)** Kuona mtima pokwaniritsa zichitochito za chipembedzo zonse. Imeneyi ndi sitepe yapamwamba kwambiri ndipo yodemerera monga kuona mtima pakuopa, chiyembekezo, kukulitsa, kusalabadira za m'dziko, kukhutitsidwa, kuyedzamira, kukonda ndi ntchito zonse za mu mtima.

Amene akhale ndi mbiri yoona mtima mu zonse zimene zatchulidwazi ndiye kuti wanenetsa zoona chifukwa choti iyeyu wapita patsogolo kwambiri poona mtima. Adanena Mtumiki (SAW) kuti : "*Dzikakamizeni kuona mtima (kunena zoona) chifukwa kuona mtima kumaongolera ku zinthu zabwino, ndipo zinthu zabwino zimaongolera ku Jannat. Ndipo munthu sasiya kunena zoona nkuonetsetsa kuti akunena zoona pokhapokha amalembedwa kwa Allah kuti wonenetsa zoona*." **(Bukhar, Muslim).**

Munthu amene choonadi chasakanizirana pa iye nakhala woona mtima kwa Allah pochifunafuna choonadicho mopanda chilakolako china cha mtima wake, nthawi zambiri amadalitsika nacho, ngati sadachipeze Allah amamukhululukira.

Mtsutso wakunena zoona ndi bodza. Ndipo choyamba cha mayendedwe a bodza chimachokera mu mtima kupita ku lirime naliipitsa kenako limayenda kunka ku ziwalo nkuipitsa ntchito zake monga m'mene limaipitsira lirime pa zoyankhula zake kotero limadzadza bodza pa zoyankhula zake, ntchito zake zachikhalidwe chake chonse choncho kuipa kumamanga nthenje pa iye.

◗ **CHIKONDI:** Kudzera mu kukonda Allah, Mtumiki wake (SAW) ndi anthu okhulupirira mumapezekamo kutsekemera (kuzuna) kwa chikhulupiriro. Adanena (SAW) kuti: "*Zinthu zitatu amene zikhale mwa iye, apeza nazo kuzuna*

*kwa chikhulupiriro. Akhale Allah ndi Mtumiki Wake okondedwa kwambiri kwa iye kuposa china chili chonse chosakhala iwo, ndikuti akonde munthu osati pa chifukwa china koma Allah ndipo adane nako kubwerera ku chikunja pambuyo poti Allah amupulutsamo momwe amayipidwira kuponyedwa mu moto*." **(Bukhar, Muslim).**

**Ukadzala mtengo wachikondi mu mtima ndikuwuthirira madzi achiyero ndikutsatira Mtumiki (SAW) ndiye kuti upatsa mitundu ya zipatso yambiri ndi zakudya zake nthawi zonse m'chifuniro cha Mbuye wake. Chikondichi chili mitundu inayi (4):**

**1.** Kukonda Allah: ili ndi pahata la chikhulupiriro.

**2.** Kukonda chifukwa cha Allah ndikuipidwa chifukwa cha Allah ichi ndiye chokakamizidwa[1].

**3.** Chikondi limodzi ndi Allah: kumeneko ndiko kumuphatikiza wina wake posakhala Allah mu chikondi chokakamiza monga kuwakonda anthu ophatikiza Allah ndi zinthu zina chifukwa cha milungu yawo, lomwe ndi tsinde la shirk.

**4.** Chikondi chachibadwa: monga kukonda makolo awiri, ana, chakudya.....zimenezi ndizovomerezeka. Ndipo kuti Allah akukonde usiye kulabadira za m'dziko. Mtumiki (SAW) adati: "*Leka kulabadira za dziko lapansi, Allah akukonda*." **(Ibn Maajah)**

**KUYEDZAMIRA (KUDALIRA):** Kumeneko ndiko kuwupereka mtima ndi kuwuyedzeka pa Allah popeza zofunikira ndi kuchotsa mavuto pamodzi ndi chikhulupiriro mwa Allah ndipo tsatira njira zovomerezeka. Kusiya kuwupereka mtima ndi nankafumbwe mu umodzi wa Allah, ndipo kusiya njira zopezera zinthu ndi kulephera komanso kupunguka nzeru. Malo ake (akuyedzamira) ali poti iwe usadachichite chinthu ndiponso chimenechi ndi chipatso cha chitsimikizo. Tsono mitundu yake (yakudalira) ilipo itatu:

---

[1] **Ndipo anthu kumbali yachikondi kapena kuipidwa (kupalana ubwenzi ndi kusiyana nawo) kuli mu zigawo zitatu (3):**

**a)** Pali amene amakonda chikondi chenicheni choyera mopanda udani awa ndi anthu amene ali okhulupirira, oyeretsedwa monga Atumiki ndi onenetsa zoona mtsogoleri wawo ndi Bwana wathu Muhammad (SAW) ndi akazi ake, ana ake achikazi, maswahaaba ake.

**b)** Anthu amene ali ongoipidwa basi: awo ndi makafiri, mamushrikuuna ndi achiphanaso.

**c)** Amene amakonda mbali ina ndikuida inzakeyo: awa ndiye olakwira malamulo m'Chisilamu. Choncho okondedwa chifukwa cha chikhulupiriro chawo ndipo odedwa chifukwa cha machimo awo.

**Kuwakonda makafiri ndikupalana nawo ubwenzi kuli mitundu iwiri:**

**1)** Komwe kumapangitsa munthu kutuluka ku Chisilamu: kumeneko ndiko kupalana ubwenzi pa chipembedzo chawo.

**2)** Komwe kuli koletsedwa koma sikutulutsa m'Chisilamu: komwe kuli kupalana ubwenzi pa zinthu zawo za m'dziko.

Ndipo nthawi zina kumapezeka kusakanizirana pakati pa kukhalirana nawo bwino makafiri (amene sathira nkhondo Asilamu ndikukondana nawo komanso kuwasasa. Kumaonekera kusiyanitsa pakati pa mbali ziwirizi motere: kuchita nawo chilungamo ndikukhalirana nawo mwa ubwino mopanda chikondi chobisika cha mu mtima monga kuchitira chifundo ofooka mwa iwo, kuyankhulana nawo liwu lodekha munjira yowachitira chisoni , izi ndi zololedwa. Allah Wolemekezeka wati: "*Allah sakukuletsani za anthu amene sanakuthireni nkhondo mu chipembedzo ndipo sanakutulutseni m'nyumba zanu kuti muwachitire zabwino ndikuwachitira chilungamo*." Tsono kudana nawo ndikuwathira udani ndi chinthu china chomwe Allah nkuyankhula kwake wati: "*Eh inu amene mwakhulupirira! Musachite adani anga komanso adani anu kukhala abwenzi nkumaponyerana nawo (mawu) mwachikondi*." Ndiye n'kutheka kuchita chilungamo pokhalirana nawo pamodzi ndikudana nawo ndikupanda kukondetsetsana nawo m'mene amachitira Mtumiki (SAW) ndi Ayuda a ku Madina.

**1.** Kokakamiza (kwa waajib): kumeneko ndiko kuyedzamira pa Allah pa chinthu chomwe wina sangathe kuchichita kupatula Allah monga kuchiza matenda.
**2.** Koletsedwa (kwa Haraam): **uku kuli mitundu iwiri:**
**a)** Shirk yaikulu: kumeneko kudalira kwa mtundu wonse njira zopezera zinthu ndikuti njirazo mwa izo zokha zimabweretsa thandizo kapena kuchotsa vuto[1].
**b)** Shirk yaing'ono monga kuyedzamira kwa munthu pokupatsa rizq popanda chitsimikizo, kudalira kwake kwa iye kuti rizq lipezeke. Koma kumati kulumikizana nalo kuti iyeyo ndi njira chabe.
**3.** Kovomerezeka : kumeneko ndiko kupereka ntchito munthu kwa wina wake ndikumudalira pa chinthu chimene iye angathe kuchichita monga kugula ndi kugulitsa. Koma zosavomerezeka kunena kuti: 'ndayedzamira pa Allah kenako pa iweyo'. Koma anene kuti: 'ndapereka ntchito kwa iwe'.

◗ **KUYAMIKA:** Kumeneku ndiko kuonetsera zisonyezo za mtendere wa Allah umene uli pa kapolo mu mtima mwake mwachikhulupiriro komanso pa lirime lake moyamika, komanso mu ziwalo zake pochita ibaadat.
Kumakhala kuthokoza ndi mtima, lirime ndi ziwalo. Tanthauzo loyamika ndiko kugwiritsira mtendere pa zinthu zomumvera Allah.

◗ **KUPIRIRA:** Kumeneko ndiko kusiya kudandaulira wina wake mavuto posakhala Allah – kuwawa kwa mavuto- ndikupereka zonse kwa Allah. Adanena Allah Tabaarakaat Wataalaa: "Ndithudi adzapatsidwa opirira malipiro awo mopanda kuwerengedwa." Ndipo Mtumiki (SAW) adati: "*Munthu amene*

---

[1] **Kodi kutsata njira zopezera zinthu ndikudalira Allah zimatsutsana? Zili ndi njira zitatu:**
**1.** Kubweretsa chithandizo chosoweka komwe kuli mu zigawo ztatu:
**a)** Njira yotsimikizika monga ukwati pofuna mwana. Kusiya njirayi (kufuna mwana popanda kukwatira) imeneyo ndi misala ndipo palibe kuyedzamira pa Allah pamenepa.
**b)** Njira zopezera zinthu zosatsimikizika koma nthawi zambiri njira zoti zipezeke izi sizingapezeke popanda zimenezi. Mwachitsanzo munthu akuyenda m'chipululu wopanda phoso. Zochita zakezi sizili mu gulu lodalira Allah ndipo kutenga kwake phoso ndikumene adalamulidwa. Ndithu Mtumiki (SAW) adali kutenga phoso ndipo adalemba ntchito munthu wolondolera njira yopita ku Madina.
**c)** Njira zopezera zinthu zomwe zimaganiziridwa kuti zikupezeka pokwaniritsa zofunikira pa zopezera zinthu mopanda chitsimikizo choonekera monga munthu amene akuwerengera zikonzero zozama pofunafuna kupezera ntchito ndi njira zake. Ndithu ameneyo sakusiya njira zoyedzamira kwa Allah. Koma kusiya kugwira ntchito mulibemo tanthauzo loyedzamira pa Allah.
**2.** Kusunga chimene chapezeka: munthu amene wapeza phoso m'njira za halaal iye nkulisunga phosolo sikungam'tulutse m'gulu loyedzamira makamaka akakhala nalo banja. "*Ndithudi Mtumiki (SAW) ankagulitsa mitengo ya kanjedza ya Banuu Al Nadhwiir nasungira banja lake chakudya cha chaka chonse.*" **(Bukhar, Muslim).**
**3.** Kutchinga vuto lisadadze mulibe lamulo m'malamulo odalira Allah. Kusiya njira zotchingira mavuto monga kuvala zibiya zankhondo, kumangirira ngamira pachingwe ndipo nkumadalira pa zonsezi yemwe amachichititsa kuti zinthu zichitike osati njirazo ndipo akhale wokhutitsidwa ndi chili chonse chimene aweluze pa iye.
**4.** Kuchotsa vuto limene ladza: kumeneku kuli ndi zigawo zitatu:
**a)** Kukhala chochotsa chimenecho: monga madzi m'mene amachotsera ludzu, ndipo kusiya ichi mulibemo tanthauzo lina lili lonse loyedzamira pa Allah.
**b)** Kukhala chongoganizira: monga kudula litsipa ndi zina zotero. Kupanga zimenezo sizikutsutsana ndi kuyedzamira pa Allah. Ndithudi Mtumiki (SAW) adalandirako mankhwala ndipo adalamula zakumwa mankhwala.
**c)** Kukhala njira zongopeka monga kudziwotcha ndi moto nthawi imene uli bwinobwino kuti usadzadwale: kupanga zimenezi kukutsutsana ndikudalira Allah.

*angadzipiriritse, Allah amupiriritsa, palibe munthu amene wapatsidwa chopatsidwa chabwino komanso chachikulu kuposa kupirira*." **(Bukhar, Muslim).**
Adanena Omar (RA) kuti: 'Palibe pamene ndidayesedwako ndi mayeserero alionse pokhapokha kuti Allah ali nane madalitso okwana anayi: ngati sali mu chipembedzo mwanga, ndipo sali akulu kwambiri, komanso ngati sindinamanidwe kukhutira ndiponso ngati ndikulakalaka kupeza malipiro pa mavutowo.
Ndipo kupirira kuli m'masitepesitepe:

- Yapansi: kumeneko ndiko kusiya kudandaula kwinaku pali kudana nazo.
- Yapakatikati: kumeneko ndiko kusiya kudandaula pamodzi ndi chisangalalo.
- Yapamwamba: kumeneko ndiko kuthokoza Allah pa mayeserero.

Amene waponderezedwa namuchitira duwa wopondereza uja kuti apeze masautso ndiye kuti wadzibwezerera, ndipo watenga gawo lake lobwezera komanso sadapirire. Kupirira kuli mitundu iwiri:

**1)** Kwa thupi: uku sicholinga chathu panopa.
**2)** Kwa mtima: pa zilakolako zachibadwa komanso zofunikira zazilakolako[1].

Ndipo chili chonse chokumana nacho kapolo pa dziko lapansili sichisowamo mitundu iwiri:

**a)** Chomwe chikugwirizana ndi chilakolako choncho munthu amasoweka kupirira pochita chofunika kum'chitira m'menemo Allah pothokoza ndipo sapereka kali konse kam'menemo pa ntchito yolakwira Allah.
**b)** Zonwe zikusemphana ndi chilakolako zomwe zili m'magawo atatu:

**i.** Kupirira pomumvera Allah: chofunikira m'menemo ndiye kuchita chinthu chokakamizidwa ndipo chabwino ndiko kuchita zinthu za sunnat,
**ii.** Kupirira posiya ntchito zochimwira Allah: chili waajib pamenepa ndiko kusiya chinthu cha Haraam – choletsedwa. Chili mustahabb mwa izo kusiya cha makrouh.
**iii.** Kupirira pa zikonzero za Allah: cha waajibu mu zimenezo ndiko kulimanga lirime pa zinthu zomwe sizim'kondweretsa Allah monga kufuula, kung'amba mmalo ovalira zovala, kumenya masaya ndi zina zotero. Chomwe chili mustahabb m'menemo ndiko kukhutitsidwa ndi mtima pa zinthu zimene Allah wazilinganiza.

**Ndi ndani ali wabwino kuposa mnzake wolemera wothokoza kapena wosauka wopirira?** Wolemera akachipereka chuma chake mu zinthu zomvera Allah kapena wachisungira kuti adzatero, ndiye kuti iye ngwabwino kuposa wosaukayu. Koma ngati wolemerayu maonongedwe ambiri a chuma chakecho amakhala pa zinthu za mubaah ndiye kuti wosaukayu ngwabwino kuposa iye. Mtumiki (SAW) adati: "*Wakudya nkuyamika ali ofanana ndi womanga wopirira*." **(Ahmad).**

**KUKHUTITSIDWA:** Kumeneko ndiko kukhutitsidwa ndi chinthu ndikukwaniritsidwa nacho. Malo ake ndi pambuyo popezeka chochitika.

[1] Mtundu um enewu kukakhala kupirirako kudziletsa chilakolako cha mimba ndi maliseche kumatchedwa kudzisunga. Kukakhala pa nkhondo kumatchedwa ukadziotche. Kukakhala poumanga mkwiyo ndikusauwonetsera, kumatchedwa kuleza. Kukakhala pobisa chinthu, kumatchedwa kusunga chinsinsi. Kukakhala pa umoyo wa munthu wamba –wosasakaza- kumatchedwa kusalabadira za m'dziko. Kukakhala pa chinthu chochepa mu zinthu za pa zdiko lapansi kumatchedwa kukhutitsidwa

Kukhutitsidwa ndi chikonzero cha Allah kuli m'gulu lopambana kwambiri pa anthu amene ali ndi malo oyandikitsidwa kwa Allah. Kukhutitsidwaku kuli m'gulu la zipatso za chikondi ndikudalira. Ndipo kupempha Allah kuti akuchotsere choipa sikukutsutsana ndi kukhutitsidwa ndi Iyeyo.

**KUDZICHEPETSA:** Kumeneko ndko kukuza, kuswedwa ndi kudzichepetsa. Adanena Huzaifah (RA) kuti: "Dzitalikitseni ku kudzichepetsa kwa uchiphamaso." Ndipo zidanenedwa kwa iye kuti: 'Kodi kudzichepetsa kwa uchiphamaso nkotani?'Ndipo iye adati: 'Iweyo kuliona thupi likudzichepetsa pamene mtima siukudzichepetsa.' Ndipo Huzaifah (RA) adati: "Choyamba chimene mumandisowa mu chipembedzo mwanumu ndikudzichepetsa." Ibaadah ili yonse yomwe yalamulidwa mkati mwake muli kudzichepetsa, ndithudi malipiro a ibaadah imeneyo amapezeka mofanana mulingo wakudzichepetsa pakutero mwachitsanzo Swalaat. Ndithudi Mtumiki (SAW) adanena zokhudzana za munthu woswali kuti alibe kalikonse mu Swalaat yakeyo kupatula theka , kapena theka la theka kapena kachigawo kamodzi mwa magawo asanu kapenanso kagawo kamodzi mwa magawo khumi koma kuti nkutheka alibiretu kalikonse mu Swalaat yakeyo.

**CHIYEMBEKEZERO:** Kumneko ndiko kuyang'ana kukula kwa chifundo cha Allah. Mtsutso wake ndi kutaya mtima. Kugwira ntchito pachiyembekezero ndikwapamwamba kwambiri kwa munthu kuposa kuigwira akuopa chifukwa choti chiyembekezero chimabala kumuganizira zabwino Allah. Allah akunena kuti: "Ine ndili pamaganizo amene kapolo wanga ali nawo pa Ine." (Muslim). Chiyembekezerochi chili m'masitepe awiri:

**1)** Yapamwamba: Amene wagwira ntchito yomvera Allah uku akuyembekezera malipiro a Allah. Aisha (RA) adafunsa: 'Eh Iwe Mtumiki (SAW) ! "*Ndipo amene akuchita zimene akuchita uku mitima yawo ikuopa" kodi ndi amene akuchita chigololo, kumwa mowa,uku akumuopa Allah?' Mtumiki adati: "Sichoncho Eh iwe mwana wamkazi wa Al Swiddeeq! Koma iwowo ndi anthu amene amaswali, kumanga, kupereka chopereka uku iwo akuopa kuti mwina ntchito zawo sizilandiridwa kuchokera kwa iwo. "Iwo ndi amene akufulumizitsira mu zinthu zabwino*." **(Tirmidhi).**

**2)** Yapansi: wochimwa wolapa amene akulakalaka chikhululuko cha Allah. Tsono wochimwa waliuma pa machimo, wosiya kulapa uku akulakalaka chifundo cha Allah, uku ndikulakalaka chabe osati chiyembekezero. Mtundu umenewu ndi wosambulidwa pamene woyamba uja ndi wotamandika. Tsono wokhulupirira weniweni ndi amene amasakaniza kuchita zabwino ndi kuopa pamene mchiphamaso amasakaniza kuipitsa ndikudziikanso pa chitetezo kuti masautso sangamkhudze.

**MANTHA:** Uku ndikusakhazikika kumene kumapeza mtima poyembekezera choipa. Ngati choipa chatsimikizika kumatchedwa mantha ndipo mtsutso wake ndi mtendere. Mantha si mtsutso wa chiyembekezero koma ndi chinthu chomwe chimadzetsa chiyembekezerocho mu njira ya kuopa pamene chiyembekezero chimadzutsa mu njira ya chikhumbokhumbo. Payenera kuphatikiza pakati pa chikondi, mantha ndi chiyembekezero. Ibn Al Qayyim adati:

“Mtima pa mayendedwe ake wopita kwa Allah uli ngati m’mene mbalame ilili. Chikondi ndi mutu wake, mantha ndi chiyembekezero ndiwo mapiko ake. Ngati mantha atakhazikika mu mtima, amakaotcha malo ake onse azilakolako nkukathamangitsa dziko lapansi m’menemo.”

Mantha a waajibu: ndi amene akumuchititsa munthu kuchita ntchito zonse zokakamizidwa (za waajibu) ndikusiya zonse zoletsedwa (za haraam).

Tsono mantha a mustahabb: awa ndi amene amachititsa munthu kuchita zinthu zomwe zili sunnat ndikusiya zinthu za makrouh.

Tsono kuopa zinthu zina zosakhala Allah kuli m’magawo angapo:

**1)** Shirk yaikulu: awa ndiwo mantha achinsinsi ndikupembedzedwa (kuchitidwa umulungu) zomwe zikuyenera kukhala za Allah basi monga kuopa milungu ya opembedza mafano kuti ingapereke masautso kapena kupezetsa munthu vuto.

**2)** Shirk yaing’ono: uku ndiko kusiya kuchita chinthu cha waajib kapena kuchita chinthu choletsedwa ( cha Haraam) chifukwa choopa anthu.

**3)** Wololedwa: monga mantha achibadwa monga kuopa tchimo ndi zina zotero.

**KUSALABADIRA ZA M’DZIKO (AL-ZZUHD):** Kumenko ndiko kuchotsa chikhumbokhumbo ku chinthu china chake ndikuchipititsa ku chinthu chimene chili chabwino kuposa chinthu chimenecho. Kusalabadira za pa dziko kumapatsa mtima ndi thupi mpumulo. Tsono kufunitsitsa za pa zdiko kumachulukitsa mangawa ndi madandaulo. Kukonda dziko la pansi ndi mutu wa tchimo lili lonse ndipo kulida dzikoli ndi njira yakumvera Allah pa kalikonse. Kusalabadira za pa dziko lapansi ndiye kuti ulitulutse dzikolo mu mtima mwako osati kulitulutsa mu dzanja lako pamene mtima walumikizana nalo- uku ndiko kusalabadira za pa dziko lapansi kwa mbutuma. Mtumiki (SAW) adati: “*Chikhalirenji bwino chuma chabwino cha munthu wabwino!”* **(Ahamad).**

Munthu wosauka, pachuma ali m’machitidwe asanu:

**1)** Akuthawa kutenga chuma chifukwa chodana nacho ndikudzitalikitsa ku zoipa zake ndi kutanganitsidwa kwake. Munthu wamachitidwe oterewa amatchedwa Zaahid (wosalabadira za m’dziko).

**2)** Asasangalalire kulipeza dziko lapansi komanso asalide kulida kodzivutitsa yekha. Munthu wotereyu amatchedwa wosangalatsidwa.

**3)** Kukhala kupezeka kwa chuma kwa iye kokondeka kuposa kusapezeka chifukwa cha chikhumbokhumbo chake mu chumacho, koma sadafike pa khumbo lake poimirira kuchifunafuna koma kuti chitam’fikira mwa ngozi amachitenga nkusangalalira nacho. Ngati atafunikira kuvutikira pochifunafuna chumacho, iye sachigwirira ntchito. Mwini mchitidwe woterewu amatchedwa wokhutitsidwa.

**4)** Kukhala koti kusiya kwake kuchifunafuna chumacho gwero lake ndikulephera kwake apo ayi, iye akuchikhumba chumacho; iye atati wapeza njira yochifunira movutikira bwenzi atachifunafuna. Munthu wotereyu amatchedwa wakhama.

**5)** Kukhala kuti wapanikizidwa ndipo wasimidwa pa zomwe watsimikiza kuzipeza mu chuma monga munthu wanjala, komanso wausiwa pofunafuna chakudya ndi chovala. Munthu wotereyu amatchedwa wosimidwa.

# KUKAMBIRANA MWACHIFATSE

Munthu wina dzina lake Abdullah adakumana ndi munthu wina dzina lake Abdun Nabi, Abdullah (dzina lomwe likutanthauza kuti kapolo wa Allah) sanalione bwino dzina limeneli lonena kuti Abdun-nabiyy, (kapolo wa Mneneri) ndipo anati "Zikutheka bwanji wina wosakhala Allah kupembedzedwa?"Kenako anamuyankhula Abdun Nabi ponena kuti: “Kodi umapembedza wosakhala Allah ?” Abdun Nabi anati" Ai, Ine sindimapembedza chosakhala Allah, ndine Msilamu ndipo ndimapembedza Allah Yekha basi. Abdullah anati." Ngati zili choncho zikukhala bwanji kukhala ndi dzina lofanana ndi maina a Akhristu, akamapatsana maina amanena kuti Abdul Maseeh (kapolo wa Yesu) ndipo sizachilendo pakuti Akhristu amam’pembedza Yesu, (AS), ndipo amene angamve dzina lako m'mutu mwake zitha kufika zoti iwe umam’pembedza Mneneri ndipo chimenecho si chikhulupiriro cha Msilamu mwa Mneneri wake, koma zofunika kwa iye ndi zoti akhulupirire kuti Muhammad (SAW) ndi kapolo wa Allah komanso Mtumiki Wake (SW)." **Abdun-nabiyy** anati, Koma Mneneri Muhammad (SAW) ndi wabwino koposa anthu onse komanso ndi Bwana wa Atumiki (AS) ndipo ife tikutchedwa ndi dzina limeneli pofuna madalitso ndi kudziyandikitsa kwa Allah (SW) kudzera mu ulemerero wa Mneneri Wake, ndi kulemekezeka kwake pa maso pa Iye, ndipo tikupempha kuchokera kwa iye (SAW) Du'aa ya zimenezo kudzera mwa iye (SAW), ndipo usadabwe; pakuti achimwene anga dzina lawo ndi Abdul Husain, ndipo patsogolo pake, abambo anga anatchedwa dzina loti Abdul Rasul. Ndipo kutchedwa maina amenewa ndi kwa kalekale ndiponso kofalikira pakati pa anthu, ndipo ndithu tidawapeza makolo athu pa zimenezi, choncho usakhwimitse pa nkhani imeneyi, pakuti zimenezi n'zopepuka komanso Deen ndiyopepuka. Ndipo Abdullah anati kumenekunso ndi kuipa kwina komwe kuli kwakukulu koposa koyamba koti umpemphe amene sali Allah zoti iye sangathe koma Allah Yekha, ndi chimodzimodzi ngakhale wopemphedwayo ndi Mneneri Muhammad'yo (SAW) kapena wosakhala iye (SAW) mwa anthu ochita zabwino zotsikirapo, monga Hussain (RA) kapena wina wake, ndipo zimenezo zikutsutsana ndi Tauheed yomwe talamulidwa ife kuitsatira, komanso zikutsutsana ndi tanthauzo la mau onena kuti "Palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma Allah." Ndipo posachedwapa ndikufunsa mafunso ena kuti kuonekere bwino kwa iwe kukula kwa zimenezi komanso mathero a kudzitcha dzina limeneli ndi ofanana ndi limeneli, ndipo ndilibe cholinga china koma choonadi ndikuchitsatira, kulongosola chabodza ndi kuchipewa, kulamulira zabwino ndi kuletsa zoipa, ndipo Allah ndiye Wopemphedwa thandizo ndi kuyedzamiridwa, ndipo palibe nzeru yosiyira zoipa ngakhale mphamvu yochitira zabwino pokhapokha kudzera mwa Allah, koma ndisadatero ndikukumbutsa mau a Allah onena kuti "*Ndithu yankho la Asilamu akaitanidwa kwa Allah ndi Mtumiki Wake kuti aweruze pakati pawo, silikhala lina koma kunena kuti "Tamva ndipo titsatira*" **(Surat 24:25)** ndinso mau Ake (SW) onena kuti: "*Choncho ngati mutatsutsana pa chinthu chilichonse, chibwezeni kwa Allah ndi Mtumiki Wake, ngatidi mukukhulupirira Allah ndi tsiku lomaliza*" **(Surat 4:59)**

**Abdullah:** Iwe wanena kuti umakhulupirira umodzi wa Allah ndipo umachitira umboni kuti palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma Allah, kodi ungathe kundilongosolera tanthauzo lake?

**Abdun-nabiyy:** Tauheed ndiko kuti ukhulupirire zoti Allah alipo, Iye ndi amene

analenga kumwamba ndi pansi, ndi kutinso Iye ndi amene anapereka moyo, wopereka imfa, amene akuyendetsa dziko lonse, ndiponso Iye ndi Wopereka Rizq, Wodziwa, Wozindikira, Wokhoza.

**Abdullah:** Zikanakhala zokhazo kuti ndiye Tauheed basi, ndiye kuti Farao, anthu ake, Abu Jahl ndi ena otero akanakhala okhulupirira umodzi wa Allah. Chifukwa choti iwo sikuti sanali kudziwa zimenezi monga anthu ambiri ogwadira mafano, ndipo Farao yemwe anadzipatsa umbuye anali kuzindikira ndi kumakhulupirira mu mtima mwake kuti Allah alipo, ndikuti Iye ndi amene akuyendetsa dziko lonse. Ndipo umboni wake ndi mau Ake (SW) onena kuti: "*Ndipo adazitsutsa zisonyezozo mwa chinyengo ndi modzikuza chikhalirecho mitima yawo idatsimikiza*" **(27: 14).** Ndipo kuvomera kumeneku kudaonekera pamtunda pa nthawi imene kudampeza kumira.

Koma zoona zake ndi zakuti, ndithu Tauheed yomwe anatumizidwa nayo Atumiki, navumbulutsidwira mabuku ndipo ma Quraish nathiridwa nkhondo chifukwa cha iyo, ndiko kum'patula Allah pomupembedza. Ndipo mau oti ibaadat ndi dzina lomwe limasonkhanitsa chilichonse chomwe Allah angachikonde ndikuchiyanja, monga mau ndi zichitochito zoonekera ndi zosaoneka. Mau oti Ilaahu amene akupezeka m'mau oti, "Palibe wopembedzedwa mwachoonadi koma Allah" tanthauzo lake ndilakuti: wopembedzedwa amene nkosayenera kupembedzedwa mwa choonadi kupatula Iye (SW).

**Abdullah:** Kodi ukudziwa kuti n'chifukwa chiyani Atumiki anatumizidwa pa dziko lapansi ndipo woyamba wao anali Nooh (AS)?

**Abdun-nabiyy:** Kuti adzawaitanire opembedza mafano kuti am'pembedze Allah Yekha ndi kuchisiya chilichonse kuti asam'phatikize nacho Iye (SW).

**Abdullah:** Ndi chifukwa chiyani anthu a Nooh anali kugwadira mafano?

**Abdun-nabiyy:** Sindikudziwa.

**Abdullah:** Allah anam'tumiza Nooh (AS) kwa anthu ake atabzola malire powalemekeza anthu omwe anali abwino omwe ndi Waddu, Suwaa, Yaghuth, Yaooq ndi Nasr.

**Abdun-nabiyy:** Kodi ukutanthauza kuti Waddu, Suwaa ndi ena otero anali maina a anthu ochita zabwino ndikuti sanali maina a makafiri odzitukumula?

**Abdullah:** Inde , maina amenewa ndi a anthu ochita zabwino, anthu a Nabi Nooh (AS) anawasandutsa kukhala milungu ndipo Arabu anawatsatira zimenezo, ndipo umboni wa zimenezo ndi mau omwe anadza kuchokera kwa Ibn Abbas (RA) iye anati "Mafano amene analipo mu nthawi ya anthu a Nabi Nooh (AS) pambuyo pake anadzapezekanso mwa Arabu. Tsopano mulungu wotchedwa Waddu anali wa banja la Kalbi yemwe anaikidwa pa malo wotchedwa Dumat-ul- Jan'dal. Tsono Suwaa anali mulungu wa kubanja la Hudhail, pamene Yaghuth anali mulungu wa banja la Murad, kenako anadzakhala wa banja la Ghutwaif, anaikidwa pamalo wotchedwa Jurf ku Saba'a. Tsono Yaooq anali mulungu wa banja la Hamdan, tsopano Nasr anali mulungu wa banja la Himyar la anthu oboola m'makutu; Awa anali maina a anthu omwe anali ochita zabwino kuchokera mu anthu a Nabi Nooh (AS), choncho atamwalira akuluakuluwo Satana anawanong'oneza anthu a Nabi Nooh (AS) kuti muzike m'malo awo omwe anali kukhalamo mafano ndipo muwatche ndi maina awo, choncho anachita zimenezo, ndipo sanagwadiridwe, kufikira pamene anthu amenewo anamwalira ndi kufufutika kuzindikira kwa cholinga chake, mafanowo anayamba kupembedzedwa" **(Bukhaari)**

**Abdun-nabiyy:** Mau awa ndi odabwitsa.
**Abdullah:** Kodi ndikusonyeze mau odabwitsa kwambiri kuposa amenewo, kuti udziwe kuti womaliza wa Aneneri Bwana wathu Muhammad (SAW) ndithu Allah anamtumiza iye kwa anthu amene amapempha chikhululuko, amachita ibaadat, amachita Twawaaf,nkumayenda pakati pa Swaafat ndi Marwat amachita Hajj ndiponso amapereka sadaka, koma kuti iwo amazichita zina zolengedwa kukhala amkhala pakati a pakati pawo ndi pakati pa Allah, amayankhula kuti" Timafuna kuchokera kwa iwo kudziyandikitsa kwa Allah ndipo timafuna pempho lawo kwa Iye Allah, monga angero, Issa (AS) ndi anthu ena ochita zabwino pa iwo. Choncho Allah anamutuma Muhammad (SAW) kuti adzawalongosolerenso bwino chipembedzo cha bambo wao Ibrahim (AS) ndikudzawauza kuti kudziyandikitsa kumeneku ndi kukhulupirira ndi ufulu wa Allah Yekha basi sizingatheke kum'chitira wina wosakhala Allah. Pakuti Iye ndi Mlengi yekhayo alibe wothandizana Naye, palibe wopereka rizq koma Iye. Mitambo isanu ndi iwiri ndi zomwe zili m'menemo komanso nthaka zisanu ndi ziwiri ndi zomwe zili m'menemo onsewo ndi akapolo Ake (SW) alinso pansi pa ufumu Wake ndi mphamvu Zake, komanso ngakhale milungu imene akuipembedzayo imavomera kuti ili pansi pa ulamuliro Wake.
**Abdun-nabiyy:** Mau amenewa ndi oopsa kwambiri komanso odabwitsa, nanga umboni wake ulipo?
**Abdullah:** Maumboni ndi ambiri ena mwa iwo ndi mau Ake (SW) oti: "*Nena: Kodi ndani akukupatsani rizq kuchokera kumwamba ndi pansi? Nanga ndani amakupatsani kumva ndi kupenya? Nanga ndani amene akutulutsa chamoyo kuchokera mu chakufa, ndikutulutsa chakufa mu chamoyo? Nanga ndani akukonza zinthu zonse? Anena, ndi Allah, choncho, nena: Kodi bwanji simukuopa?"* **(Surat 10:31).** Ndi mau Akenso (SW) onena kuti: "*Nena: "Kodi nthaka ndi yandani ndi zomwe zili m'menemo, ngati inu mukudziwa" adzanena kuti: "Ndi za Allah;" Nena: "Nanga bwanji simukunkumbukira". Nena: "Kodi ndani Mbuye wa thambo zisanu ndi ziwiri, ndinso Mbuye wa Mpando waukulu?" Anena kuti; "Ndi za Allah"; Nena: "Nanga bwanji simukumuopa?" Nena: "Kodi ndani Yemwe m'manja Mwake muli mphamvu yolamulira chinthu chilichonse? Ndipo Iye amateteza zonse, ndipo palibe chimene chingatetezedwe ku chilango Chake ngati inu mukudziwa?" Anena kuti "Ndi Allah." Nena: "Nanga mukulodzedwa bwanji ndi Satana?* **(Surat 23: 84 - 89).** Ndipo anthu opembedza mafano pochita Hajj anali kuitana ndi mau awo onena kuti: "Mulibe wothandizana naye kupatula wothandizana yemwe ali Wanu, za iye ndi iye yemwe zili m'manja Mwanu. Choncho kuvomera kwa mamushrik Achiquraish zoti Allah ndi amene amayendetsa dziko, kapena kuvomera zomwe zimatchedwa kuti Tauheed ya uleri komwe ndi kuvomera kumeneko sikunawalowetse m'Chisilamu. Ndipo kufuna kwao Angero kapena aneneri kapena maWaliy amafuna kuti iwo akawanenere kwa Allah ndi kudziyandikitsa kwa Allah ndi zimenezo, ndi zomwe zinapangitsa Halaal kukhetsedwa mwazi wao komanso kulandidwa chuma chawo. Pa chifukwa chimenecho n'zofunika kuipereka Du'aa ina iliyonse kwa Allah, lonjezo lililonse kwa Allah, kuzinga kalikonse kwa Allah. Kupempha thandizo kulikonse kudzera mwa Allah, ndi mitundu yonse ya ibaadat kukhala ya Allah.
**Abdun-nabiyy:** Ngati Tauheed siili kuvomera kuti Allah alipo ndi kulamulira Kwake dziko monga ukunenera, nanga Tuheed ndi chiyani?

**Abdullah:** Tauheed yomwe anatumizidwira Atumiki ndikukana kuivomera anthu opembedza mafano ndiyo kum'patula Allah pakum'chitira ibaadat, motero chisaperekedwe china chili chonse m'mitundu ya ibaadat kwa china chake chosakhala Allah. Monga Du'aa, lonjezo, kuzinga, kupempha chipulumutso, kupempha thandizo ndi zina zotero. Ndipo Tauheed imeneyi ndiyatanthauzo la kuyankhula kwako konena kuti:"**LAILAHAILLALLAH**" palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma Allah, pakuti amene adali mulungu kwa ma Quraish opembedza mafano ndi amene anali kuchitiridwa ibaadat imeneyi. Chimodzimodzi anali mngero kapena Mneneri, kapena Waliyy, kapena mtengo, kapena manda kapenanso chiwanda, ndipo sanali kutanthauza kuti Mulungu wa fano ndiye mlengi, wopereka rizq, wokonza zinthu, pakuti iwo anali kuzindikira kuti zimenezo ndi za Allah Yekha monga zanenedwera kale. Choncho Mneneri (SAW) anawadzera iwo kudzawaitanira iwo ku liwu la umodzi wa Allah lonena kuti palibe wopembedzedwa mwachoonadi koma Allah Yekha ndi kugwiritsira ntchito tanthauzo lake osati kungoliyankhula basi.

**Abdun-nabiyy:** Ukukhala ngati ukufuna kunena kuti ma mushrik achi Quraish anali kudziwa kwambiri tanthauzo la mau oti **LAA ILAHA ILLALLAH** kusiyana ndi Asilamu ambiri omwe tili nao masiku ano.

**Abdullah:** Inde, zimenezo ndi zoona zokhazokha zomwe zili zopweteka kwambiri, chifukwa makafiri omwe ali ambuli amadziwa kuti cholinga cha Mneneri (SAW) ndi liwu limeneli ndi kumpatula Allah pakum'pembedza, ndi kuchikana chomwe chimapembedzedwa pambali pa Allah ndi kudzitalikitsa nacho, pakuti iye (SAW) nthawi imene anawauza iwo kuti nenani mau oti LAA ILAAHA ILLALLAH, iwo anati; "*Akuichita milungu yonse kukhala Mulungu mmodzi? Ndithu chimenechi ndi chinthu chodabwitsa*" (Surat 38:5), chikhalirecho iwo amakhulupirira kuti Allah ndiye Wolamulira dziko, choncho ngati mbuli za Chikafiri zikudziwa zimenezo n'zodabwitsa tsono kwa amene akudzitcha kuti ndi Msilamu asakudziwa tanthauzo la liwu limeneli lomwe alidziwa ambuli achikafiri, koma iye akuganiza kuti Tauheed yo ndiye kuziyankhula zilembo zake mopanda kutsimikiza kwa mumtima kalikonse m'matanthauzo ake. Anzeru mwa iwo amakhulupirira kuti tanthauzo lake ndiloti palibe amene amalenga, amapereka rizq, kapena kukonza zinthu koma Allah Yekha. Choncho palibe mtendere kwa anthu amene akudzitcha kuti ndi Asilamu ndipo ambuli achikafiri achi Quraish n'kukhala ozindikira kwambiri kuposa iwo tanthauzo la mau oti LAA ILAAHA ILLALLAH.

**Abdun-nabiyy:** Koma ine sindimuphatikiza Allah ndi kena kake koma ndikuchitira umboni zoti palibe amene amalenga, amapereka rizq, amathandiza kapena kupereka vuto, koma Allah Yekhayo, alibe wothandizana Naye, ndikuikiranso umboni kuti Muhammad (SAW) alibe mphamvu yodzithandizira yekha kapena kudzipatsa vuto, nanji Al- Hussain, AbdulQaadir ndi ena otero, koma kuti ine ndi wochimwa, ndipo anthu ochita zabwino ali ndi ulemerero pa maso pa Allah ndipo ndinawapempha iwo kuti andidandaulire ine kwa Iye (SW) ndi ulemerero umene ali nawo kwa Iye.

**Abdullah:** Ndikuyankha zomwe zanenedwa kale, zoti ndithu amene adamenyana nao Mneneri (SAW) ankavomereza zomwe wanenazo, komanso ankavomereza kuti ndithu mafano awo sakonza chilichonse, ndipo ndithu adafuna anthuwo kuchokera

ku mafano awo ulemerero ndi kukawadandaulira iwo pamaso pa Allah, ndiponso zanenedwa kale, pakuti ife tapereka umboni pa zimenezo wochokera mu Qur'an.

**Abdun-nabiyy:** Koma ma Ayat amenewa adavumbulutsidwa kwa amene ankapembedza mafano, choncho ndi chifukwa chiyani mukuwachita Aneneri ndi anthu abwino kukhala ngati mafano?

**Abdullah:** Zanenedwa kale, komanso tagwirizana kuti ndithu ena mwa mafanowa anatchedwa maina a anthu abwino, monga m'mene zinalili mu nthawi ya Nooh (AS), ndikutinso makafiri sadafune chilichonse kuchokera ku mafanowa koma kukawadandaulira pa maso pa Allah, chifukwa choti mafanowo ali ndi ulemerero kwa Iye (SW), ndipo umboni pa nkhani imeneyi ndi mau Ake (SW) onena kuti; *"Koma amene adzipangira athandizi kusiya Allah ndikumanena kuti "Ife sitikuwapembedza iwo, koma tikutero ndi cholinga choti atifikitse pafupi ndi Allah"* **(Surat 39: 3).** Tsopano mau ako onena aja kuti chifukwa chiyani mukuwachita Aneneri ndi ma Waliyy kukhala mafano? Ife tikuti: ndithu makafiri omwe Mneneri (SAW) anatumizidwa kwa iwo, mwa iwo muli amene amawapempha ma Waliyy, omwe Allah wanena za iwo kuti: "*Iwo amene akuwapempha naonso akufunafuna njira yodziyandikitsira kwa Mbuye wawo ngakhale omwe ali pafupi mwa iwo ndi Allah, monga angero naonso akuyembekezera chifundo Chake ndi kuopa chilango Chake; ndithu chilango cha Mbuye wako, nchoopedwa*" **(Surat 17:57).** Ndiponso mwa iwo muli amene amam'pempha Issa (AS) ndi mai wake, ndipo Allah wolemekezeka wanena kuti: "*Kumbukirani pamene Allah adzanena: "Iwe Yesu mwana wa Mariya: Kodi iwe udauza anthu kuti, Ndichiteni ine ndi mayi wanga monga milungu iwiri m'malo mwa Allah?"* Ndipo mwa iwo muli amene amawapempha angero, ndipo ndithu Allah Wolemekezeka wanena kuti: *"Ndipo kumbuka iwe Mneneri tsiku limene Allah adzawasonkhanitse onse ndi kunena kwa angero. "Kodi awa amapembedza inu?"* **(Surat 34:40)**

Choncho lingalirani m'ma Ayat amenewa, ndithu Allah m'ma Ayat, amenewo amunena kuti ndi kafiri amene wawapitira mafano, komanso amunena kuti ndi kafiri amene wawapitira anthu ochita bwino kuti akapeze thandizo kwa iwo 'gulu la Aneneri, angero ndi ma Waliyy mosasiyanitsa, ndipo Mtumiki wa Allah (SAW) anamenyana nao, ndipo sanasiyanitse pakati pawo pa nkhani imeneyo.

**Abdun-nabiyy:** Koma makafiri amafuna thandizo kuchokera kwa iwo, koma ine ndi kuikira umboni kuti Allah (SW) ndiye Wopereka thandizo, Wopereka vuto, woyendetsa chilichonse, ndipo ine sindifuna zimenezo kuchokera kwa wina koma kwa Iye (SW), ndipo anthu ochita zabwino alibe gawo lililonse mu zimenezi, koma kuti ndinawapitira iwowo ndi chiyembekezo choti akandidandaulira kwa Allah.

**Abdullah:** Kuyankhula kwakoku ndi chimodzimodzi ndi kuyankhula kwa makafiri chimodzimodzi. Ndipo umboni ndi mau Ake (SW) onena kuti: "*Ndipo iwo akupembedza milungu ina n'kumusiya Allah, yomwe singathe kuwapatsa masautso ngati atasiya kuipembedza, ndiponso singathe kuwapatsa chithandizo ngati atalimbika kuipembedza, ndipo akunena: "Iwo, mafanowo ndi awomboli athu kwa Allah*" **(Surat 10:18)**

**Abdun-nabiyy:** Koma ine sindipembedza chilichonse koma Allah, ndipo kuthawira kwa iwo ndi kuwapempha sikupembedza.

**Abdullah:** Koma ine ndikufunse, kodi ukuvomera kuti Allah analamula kwa iwe zomuyeretsera Iye ibaadat ndipo kuteroko ndi ufulu Wake (SW) uli pa iwe?

Monga akunenera mu mau Ake (SW) onena kuti, "*Ndipo sadalamulidwe china koma kuti am'pembedze Allah ndi kumuyeretsera chipembedzo Chake mopendekera ku choonadi*" **(Surat 98:5).**

**Abdun-nabiyy:** Inde, zalamulidwa zimenezo kwa ine.

**Abdullah:** Ndipo ine ndikupempha kuchokera kwa iwe kuti undilongosolere ine chimene Allah wachilamuliracho kwa iwe, kodi kumeneku ndiye kumuyereretsera ibaadat?

**Abdun-nabiyy:** Sindinamvetse chomwe utanthauza ndi funsoli, choncho ndiuze bwinobwino.

**Abdullah:** Tchereza khutu kwa ine kuti ndikuuze bwinobwino, Allah akunena kuti "*M'pempheni Mbuye wanu modzichepetsa ndi mwa kachetechete, Iye (SW) sakonda obzola malire.*" **(Surat 7 :55),** choncho kodi Duàa ndi ibaadat yom'pangira Allah kapena ai?

**Abdun-nabiyy:** Eya, kupemphako ndiye phata la ibaadat, monga akunenera mu Hadith kuti Duàa ndiye ibaadatyo. **(Abudawood)**

**Abdullah:** Pakuti wavomera kuti Duàa ndi ibaadat yomuchitira Allah, kenako iwe wam'pempha Allah usiku ndi usana moopa ndi mwakhumbo pa china chake chomwe ukufuna, kenako chomwe ukuchifunacho ukukam'pempha Mneneri kapena mngero kapena munthu amene anali wochita zabwino amene ali m'manda ake, kodi ndiye kuti wachita shirk mu ibaadat imeneyi?

**Abdun-nabiyy:** Eya, ndachita shirk, ndipo mau amenewa ndi owona komanso omveka.

**Abdullah:** Palinso chitsanzo china chomwe ndi choti; ukadziwa mau a Allah onena kuti "*Choncho pitiriza kupempha Mbuye wako ndipo zinga nsembe yako*" **(Surat 108: 2),** ndipo wamvera chilamulochi kuchokera kwa Allah, motero wazinga ndi kubaya chifukwa cha Iye (SW), kodi kuzinga kwako ndi kubaya kwako ndi ibaadat yom'chitira Allah kapena ai?

**Abdun-nabiyy:** Eya, imeneyo ndi ibaadat.

**Abdullah:** Choncho ngati utazinga chifukwa cha cholengedwa, Mneneri kapena chiwanda, kapena china chake pamodzi ndi Allah , kodi wasakaniza mu ibaadat imeneyi chosakhala Allah?

**Abdun-nabiyy:** Eya, imeneyi ndi shirk mosakaika.

**Abdullah:** Ndipo ine ndakupatsa chitsanzo cha Duàa ndi kuzinga, chifukwa choti Duàa ndi imodzi mwa mitundu ya ibaadat ya mau yamphamvu, ndipo kuzinga ndi imodzi mwa mitundu ya ibaadat yamphamvu ya zichitozichito, ndipo ibaadat si ziwiri zokhazi ayi , koma ibaadat ndi zinthu zambiri kuposa ziwirizi ndipo mu ibaadat'mo mukulowamo kulonjeza, kulumbira, kupempha chitetezo, kupempha thandizo ndi zina zotero. Koma anthu ogwadira mafano omwe Quràn inavumbulutsidwa mwa iwo, kodi anali kugwadira angero, anthu ochita zabwino, Laata lomwe ndi dzina la fano ndi zina zotero?

**Abdun-nabiyy:** Eya, iwo anali kuchita zimenezo, ndithu kunali kupembedza kwawo zimenezo, kupempha chitetezo , kupempha chithandizo ndi kothawira, pakuti iwo anali kuvomera kuti ndi akapolo a Allah, ndipo ali pansi pa ulamuliro Wake (SW), ndi kutinso Allah ndi amene amakonza zinthu , koma kupempha kwawo ndi kuthawira ku zimenezo n'chifukwa cha ulemelero ndi kufuna chiwombolo, ndipo zimenezi ndi zoonekera kwambiri.

**Abdun-nabiyy:** Kodi iwe Abdullah! Ukukanira chiwombolo, cha Mtumiki (SAW) ndipo ukudzitalikitsa kuchimenecho?

**Abdullah:** Ai, ine sindikuchikana chiwombolo ndipo sindikudzitalikitsa ku chimenechi, koma ndikudzipereka ine ndi makolo anga kwa iye , iye ndi muwomboli wolandiridwa chiwombolo (SAW), ndipo ndikulakalaka chiwombolo chake, koma kuti chiwombolo chonse ndi cha Allah, monga wanenera Allah kuti; "*Nena: Chiwombolo chonse chili kwa Allah*" **(Surat 39:44)**, ndipo sichingakhalepo pokhapokha pambuyo poti Allah waloleza, monga Allah wanenera kuti "*Kodi ndani angathe kuwombola kwa Iye popanda chilolezo Chake*" **(Surat 2 :255)**. Ndipo palibe amene angawomboledwe koma pambuyo poti Allah waloleza kuti zitero, monga Allah wanenera kuti: "*Ndipo sangawombole koma yekhayo amene Allah wamuyanja* " **(Surat 21:28)**. Ndipo Allah sakondwera ndi china koma Tauheed, monga Allah wanenera kuti: "*Ndipo amene angatsate chipembedzo chosakhala Chisilamu, sichidzalandiridwa kwa iye, ndipo iye tsiku lomaliza adzakhala mmodzi mwa anthu otaika*" **(Surat 3:85)**. Choncho ngati chiwombolo chonse chili kwa Allah ndipo sichingachitike koma pambuyo pa chilolezo Chake (SW). Mneneri (SAW) sadzachita Duà ya chiwombolo kapena wina wake kum'chitira wina wake mpaka Allah adzaloleze kuti zitero, ndipo Allah sadzaloleza pokhapokha kwa anthu okhulupirira za umodzi wa Allah, zikadziwika kuti chiwombolo chonse chili kwa Allah, ine ndimachipempha kuchokera kwa Iye (SW) ndipo ndimati; Eya, Mbuye wanga! Musandimane chiwombolo chake (SAW) Eya, Mbuye wanga! Kamuloleni Mtumiki wanu kukandichitira Duàa ya chiwombolo ndi mau ena otero

**Abdun-nabiyy:** Tagwirizana kuti ndithu sizikuloledwa kuti chipemphedwe kwa aliyense chinthu chimene alibe, ndipo Mneneri (SAW) Allah anam'patsa iye Duàa ya chiwombolo, tsopano chifukwa choti iye anapatsidwa Duàayo ndiye kuti ndithu alinayo ndipo pa chifukwa chimenechi zikuloledwa kuti ine ndipemphe kwa iye chimene alinacho ndipo zimenezo sizingakhale shirk.

**Abdullah:** Eya, mau amenewa ndi woona akadakhala Allah sanakuletse zimenezo, pakuti Allah akunena kuti: "*Choncho musam'pembedze aliyense pamodzi ndi Allah*" **(Surat 72:18)**. Ndipo kupempha chiwombolo imeneyo ndi Duàa, ndipo amene amam'patsa Mneneri (SAW) chiwombolo ndi Allah, ndipo Iye ndi Amene wakuletsa iweyo kuti upemphe chiwombolocho kwa wina wake mulimonse m'mene angakhalire wopemphedwayo. Ndiponso ndithu chiwombolo chimene anapatsidwa wosakhala Mneneri (SAW) ndi zoona kuti angero nawo adzapempha Duàa ya chiwombolo, naonso ana amene anamwalira asanathe msinkhu adzapempha Duàa ya chiwombolo, choncho kodi ukunena kuti ndithu Allah anawapatsa iwowa Duàa ya chiwombolo, motero ndiziyipempha kuchokera kwa iwo? Ukavomera zimenezi ndiye kuti wabwerera powapembedza anthu ochita zabwino zomwe Allah wazinena m'Bulu Lake, ndipo ukanena kuti ayi ndiye kuti mau ako ndi abodza, onena kuti. Allah wam'patsa chiwombolo ndipo ine ndikum'pempha mu zomwe Allah wam'patsa.

**Abdun-nabiyy:** Koma ine sindikum'phatikiza Allah ndi chilichonse ndipo kuthawira kwa anthu ochita zabwino si shirk.

**Abdullah:** Kodi ukuvomera motsimikiza kuti Allah analetsa shirk kwakukulu kusiyana ndi Haraam ya chiwerewere, ndikutinso Allah sangaikhululukire?

**Abdun-nabiyy:** Eya, ndikuvomera zimenezo ndipo zimenezo ndi zosabisika m'mau a Allah (SW).
**Abdullah:** Tsopano iwe panopa waitsutsa mwa wekha shirk yomwe Allah Waichita Haraam, choncho ndikukulumbirira Allah, kodi zikuloledwa kwa iwe kuti undilongosolere ine kuti ndi shirk yanji yomwe iwe sunagwemo ndipo waikana mwa iwe wekha.
**Abdun-nabiyy:** Shirk ndiye kugwadira mafano, kupereka maganizo onse ku mafanowo, kuwapempha ndi kuwaopa.
**Abdullah:** Kodi kugwadira mafano kukutanthauza chiyani? Ukuganiza kuti makafiri achi Quraish amakhulupirira kuti matabwa ndi miyala ija zimalenga, zimapereka rizq ndiponso zimakonza zinthu kwa amene wazipempha? Iwo sakhulupirira zimenezo monga ndakuuzira kale.
**Abdun-nabiyy:** Inenso sindikhulupirira zimenezo, koma amene walipitira thabwa kapena mwala kapena chiliza kapenanso china chake n'kumachipempha ndi kuzinga chifukwa cha icho, ndipo akunena kuti chimenecho chitiyandikitsa pafupi ndi Allah, ndipo Allah atiteteza kudzera m'kudalitsika kwa chinthucho, kumeneku ndiko kupembedza mafano komwe ine ndikutanthauza.
**Abdullah:** Wanena zoona, koma zimenezi ndiye zochita zanu ku miyala, zomangamanga ndi ku ziliza zomwe zamangidwa pa manda ndi zina zotero. Ndinso kuyankhula kwako konena kuti shirk ndiko kugwadira mafano; kodi tanthauzo lako kuti shirk ili kwa munthu amene wachita zokhazo? Ndikuti kuyedzamira mwa anthu ochita zabwino ndi kuwapempha zofuna zako sizikulowa m'gulu la shirk?
**Abdun-nabiyy:** Eya, zimenezo ndi zimene ndimatanthauza.
**Abdullah:** Ngati zili choncho uli pati iweyo ndi ma Ayat ambirimbiri omwe Allah watchulamo za kuletsedwa kuyedzamira mwa Aneneri ndi anthu ochita zabwino ndi angero ndi ena otero ndipo amene wachita zimenezo wamutcha kuti ndi kafiri monga zanenedwa kale, pakuti ndakuuza kale zimenezo ndiponso ndapereka umboni wake.
**Abdun-nabiyy:** Koma amene amapembedza angero ndi aneneri sanatchulidwe kuti makafiri ndi chifukwa chimenechi. koma pa zifukwa zimene iwo ananena kuti ndithu angero ndi ana akazi a Allah ndipo Yesu ndi mwana wam'muna wa Allah, ndipo ife sitinanene kuti AbdulQuadir (RA) ndi mwana wamwamuna wa Allah, ndipo Zainab ndi mwana wa mkazi wa Allah.
**Abdullah:** Tsopano kunena kuti Allah ali ndi mwana, umenewo ndi ukafiri wapadera Allah akunena kuti: "*Nena Iwe Mtumiki (SAW) Iye ndi Allah Mmodzi, Allah Wodaliridwa ndi zolengedwa zake, sanabereke ndiponso sanaberekedwe*" **(Surat 112 :1-3).** Choncho amene wakanira zimenezi ndiye kuti wasanduka kafiri ngakhale sanakanire kumapeto kwa Suratyi, ndipo Allah wanena kuti: "*Allah sadadzipangire mwana, ndipo palibe pamodzi ndi Iye mulungu wina, ndipo zikadakhala choncho ndiye kuti mulungu aliyense akadatenga zimene adalenga ndipo milungu ina ikadaipambana milungu inzake polimbirana ufumu* **(Surat 23:91).** Choncho asiyanitse pakati pa ukafiri uwiri wu Umboni winanso pa zimenezi ndi woti amene anasanduka kukhala makafiri chifukwa chopembedza fano lotchedwa Laata kumachita kuti iye anali munthu wabwino sanam'chite kukhala mwana wa Allah, ndiponso amene amasanduka kukhala makafiri chifukwa chopembedza majini sanawachite majiniwo kukhala ana a Allah, chimodzimodzi akuluakulu a Mazhab anai amanena pa mutu woti "lamulo la

munthu wotuluka Chisilamu". Msilamu akakhulupirira kuti Allah ali ndi mwana ndiye kuti watuluka Chisilamu, ndipo akam'phatikiza Allah ndi china chake ndiye kutinso ameneyo watuluka Chisilamu, ndipo akusiyanitsa pakati pa mitundu iwiriyi.

**Abdun-nabiyy:** Koma Allah akunena kuti; "*Tamverani ndithu okondedwa a Allah sadzakhala ndi mantha pa tsiku la Kiyaamat, ndipo sadzadandaula"* **(Surat 10 : 62)**.

**Abdullah:** Ifenso timakhulupirira kuti zimenezo n'zoona timanenanso zimenezo, koma sapembedzedwa, ndipo ife sitikukana chilichonse kupatula zowapembedza iwo pamodzi ndi Allah ndi kuwaphatikizanso pamodzi ndi Iye (SW) ndi zimene tikukana, koma ngati sizili choncho, ndiye kuti ukufunika kuti uwakonde ndi kuwatsatira, ndi kuvomeranso zozizwitsa zao. Ndipo palibe amene angakanire zozizwitsa za ma Waliyy kupatula anthu a Bidah, ndipo chipembedzo cha Allah chili pakatikati pa mbali ziwiri, nachonso choonadi chili pakati pa kusokera kuwiri.

**Abdun-nabiyy:** Anthu amene Quràn inavumbulutsidwa mwa iwo sachitira umboni kuti palibe wopembedzedwa mwachoonadi koma Allah, amakana Mtumiki wa Allah (SAW), amakanira za kuuka kwa akufa, amaikana Quràn ndipo amaichita kuti ndi matsenga. Pomwe ife timachitira umboni kuti palibe wopembedzedwa mwachoonadi koma Allah , ndikutinso Muhammad (SAW) ndi Mtumiki wa Allah, timaivomereza Quràn, timakhulupirira za kuuka kwa akufa ,timaswali , komanso timaamanga swaum, choncho n'chifukwa chiyani mukutiyerekeza ife ndi iwo?

**Abdullah:** Koma palibe kusiyana maganizo pakati pa ma ulama onse, kuti ndithu munthu akamuvomereza Mtumiki wa Allah (SAW) pa gawo lina ndikumukana pa gawo lina ndithu iyeyo ndi kafiri sadalowe m'Chisilamu, chimodzimodzinso akakhulupirira mbali ina ya Quran ndikukanira mbali ina, monga amene wavomereza umodzi wa Allah ndikuikanira Swalaat, kapena wavomereza umodzi wa Allah ndi Swalaat ndikukanira chikakamizo cha Zakaat, kapena wavomereza zonsezi ndikukanira Swaum (kusala), kapena wavomereza zonsezi ndi kukakanira waajibu ya Hajj, ndipo pamene anthu ena mu nthawi ya Mneneri (SAW) sanagonjere chilamulo cha Hajj, Allah Wapamwambamwamba anavumbulutsa pa nkhani ya iwo mau onena kuti "*Ndipo Allah wawalamula anthu kuti akachite Hajj ku Nyumbayo amene angathe kukonzekera ulendo wonka kumeneko. Ndipo yemwe angakane, (osapitako pomwe ali nazo zomuyenereza), ndithu Allah, ngwachikwanekwane pa zolengedwa Zake*" **(Surat 3:97)** Ngati angakanire za kuuka kwa akufa ndiye kuti wachita ukafiri mogwirizana ma Ulama onse, ndipo ndi chifukwa chake Allah wanena poyera m'Buku Lake kuti: *"Amene wakhulupirira mbali ina ya Quran nakana mbali ina, ndiye kuti iyeyo ndi kafiri weniweni"*. Ndipo zalamulidwa kuti Chisilamu chitsatiridwe chathunthu, ndipo amene watsatira china chake, nasiya china chake ndiye kuti ndithu wachita ukafiri, choncho kodi iwe ukuvomereza kuti amene wakhulupirira mbali ina nasiya mbali ina wachita ukafiri?

**Abdun-nabiyy:** Eya, ine ndikuvomereza zimenezo, ndipo zimenezo zoonekera poyera mu Quran Yolemekezeka.

**Abdullah:** Choncho ngati iwe ukuvomereza kuti amene wamuvomereza Mtumiki (SAW) pa china chake nakanira chikakamizo cha Swalaat, kapena wavomereza china chili chonse kupatula za kuuka kwa akufa, ndiye kuti iyeyo ndi kafiri mogwirizana Mazhab onse, ndipo Quran yakamba kale zimenezo, monga zanenedwa kale.Choncho

zindikira kuti Tauheed ndi Fardh yaikulu kwambiri yomwe anadza nayo Mneneri (SAW), ndipo Tauheed'yo ndi yaikulu kwambiri kuposa Swalaat, Zakaat ndi Hajj, choncho zingakhale bwanji ngati munthu atakanira kena kake mu zinthu zimenezi, atha kukhala kafiri ngakhale atagwiritsa ntchito chili chonse chomwe anadza nacho Mtumiki (SAW). Ndipo akakanira Tauheed yomwe ndi chipembedzo cha Atumiki onse sangakhale kafiri? Kuyera ndikwa Allah! Ah! Udabwitsirenji umbuli uwu?
Komanso omalingalira Maswahaaba a Mtumiki wa Allah (SAW) nthawi imene anamenyana nao a banja la Hanifah mu mzinda wotchedwa Yamaamah, kumachita kuti iwo analowa Chisilamu ndi Mneneri (SAW), ndipo iwo ankachitira umboni kuti palibe wopembedzedwa mwachoobadi koma Allah, ndikutinso Muhammad (SAW) ndi Mtumiki wa Allah, ankaswali ndiponso ankachita Azaan.
**Abdun-nabiyy:** Komatu iwo ankachitira umboni kuti Musailamah ndi Mneneri, pomwe ife tikuti: palibe Mneneri wina aliyense pambuyo pa Muhammad (SAW).
**Abdullah:** Koma inuyo mumawaika anthu ena ochita zabwino m'gulu la atumiki, angero kapena maswahaaba ndi ena otero pa ulemerero wa Allah Mwini kudzitukumula kumwamba ndi pansi, choncho zikakhala kuti kumkweza munthu pa ulemerero wa Mneneri (SAW) ndi ukafiri, ndipo chuna chake n'chololedwa kulandidwa komanso kukhetsedwa mwazi wake, ndipo mashahadah awiri kapena Swalaat sizinamuthandize, choncho amene wam'kweza munthu pa ulemelero wa Allah, ukafiri wake ndiye chizimu. Chimodzimodzi anthu amene Ali (RA)anaotcha moto onsewo anali kudzitcha kuti Asilamu, kumachita iwo anali om'konda Ali (RA) komanso anaphunzira Ilm kuchokera kwa Maswahaaba, koma kuti anali ndi chikhulupiriro mwa Ali (RA), monga chikhulupiriro chomwe muli nacho mwa AbdulQaadir ndi ena .Choncho maswahaaba anagwirizana bwanji za kuwapha iwo ndi kuwachita makafiri? Kapena ukuganiza kuti maswahaaba ankachita Asilamu anzawo kukhala makafiri kapena ukuganiza kuti kukhala ndi chikhulupiriro mwa Bwana Sayyid ndi ofanana ndi iwo kulibe vuto, ndipo kukhala ndi chikhulupiriro mwa Ali (RA) kungachititse munthu kukhala kafiri?
Komanso kuti ngati anthu oyambirira sanatchulidwe kuti ndi makafiri chabe chifukwa choti iwo anasonkhanitsa pakati pa shirk , kumtsutsa Mtumiki (SAW), Quran, kukanira za kuuka kwa akufa ndi zina zotero, nanga mutu umene autchula ma Ulama m'mazhab onse wonena kuti: "Mutu Wolongosola za munthu amene watuluka Chisilamu" ukutanthauza chiyani? Ameneyo ndi Msilamu amene amalowa ukafiri pambuyo pa Usilamu wake, ndipo anatchula zinthu zambiri, mtundu ulionse mwa zimenezo umam'tulutsa munthu m'Chisilamu, kufikira iwo anene zinthu zomwe zili zochepa kwa munthu amene wazichita, monga liwu lom'kwiyitsa Allah munthu amalinena ndi lirime lake osati ndi mtima wake, kapena analitchula liwulo mosereula ndi kusewera. Chimodzimodzinso anthu amene Allah (SW) wanena za iwo kuti: "*Nena, Mumachitira Allah, Ayat Zake ndi Mtumiki Wake zachipongwe? Musalandule, ndithu mwaonetsera ukafikiri wanu poyera pambuyo pa chikhulupiriro chanu (chabodza).*" **(Surat 9: 65-66).** Choncho Anthu awa amene Allah wanenetsa kuti ndi makafiri pambuyo pa chikhulupiriro chawo chikhalirecho anali limodzi ndi Mtumiki Wake (SAW) ku nkhondo ya Tabook, ananena liwu lomwe adanena kuti adangolinena mosereula.

Zimanenedwanso kuti zomwe Allah anasimba zokhudza ana a Israel chikhalirecho anali Asilamu ndi kuzindikira kwao ndinso kuchita kwao zabwino kuti iwo anati kwa Mussa: "*Nafenso tipangire mulumgu*" (Surat 7:138) ndi kuyankhula kwa anthu ena mwa Maswahaaba a Mneneri (SAW) konena kuti tipangireni mtengo woyedzeka zida za nkhondo.

Choncho Mneneri (SAW) analumbirira kuti zimene mukunenazi zili ngati zimene amayankhula ana a Israel kuti tipangireni milungu monga iwo ali ndi milungu.

**Abdun-nabiyy:** Koma ana a Israel komanso (Maswahaabat) amene anamupempha Mneneri (SAW) kuti awapangire mtengo woyedzeka zida sanakhale makafiri chifukwa cha zimenezo.

**Abdullah:** Ndipo yankho ndiloti: ana a Israel komanso amene anamupempha Mneneri (SAW) sanachite zimenezo, ndipo akanachita zimenezo akanakhala makafiri, ndikuti amene anawaletsa Mneneri (SAW) akanapanda kumumvera iye (SAW) ndikupanga mtengo woyedzeka zida pambuyo poti iye (SAW) waletsa akanakhala makafiri.

**Abdun-nabiyy:** Koma ine sindimvetsa penapake mu nkhani ya Usaamat bin zaid (RA) pamene anamupha amene ananena mau oti LAA ILAAHA ILLALLAH ndi kuipidwa kwa Mneneri (SAW) pa zimenezo ndipo anati kwa iye: "*Eya, iwe Usaamat wamupha pambuyo poti wanena mau oti LAA ILAAHA ILLLALLAH?* (Bukhaari). Ndinso mau ake Mtumiki (SAW) onena kuti: "*Ndalamulidwa kuti ndilimbane ndi anthu kufikira atayankhula mau oti LAA ILAAHA ILLALLAH." Choncho ndingaluzanitse bwanji pakati pa zomwe wanena ndi ma Hadith awiriwa?* Ndiwongolereni Allah akuwongola.

**Abdullah:** Ndizachidziwikire kuti Mneneri (SAW) anamenyana ndi Ayuda ndi kuwagwira ukapolo chikhalirecho amanena kuti LAA ILAAHA ILLALLAH. Ndikutinso Maswahaaba ake (SAW) anamenyana ndi banja la Hanifah chikhalirecho amaikira umboni wonena kuti palibe wina wopembedzedwa mwa choonadi koma Allah ndikuti Muhammad (SAW) ndi Mtumiki wa Allah, ndiponso ankaswali, chimodzimodzinso anthu amene Ali (RA) anawatentha moto. Ndipo iwe ukuvomera kuti amene wakanira za kuuka kwa akufa wachita ukafiri ndipo akulolewa kuphedwa ngakhale atanena mau oti LAA ILAAHA ILLALLAH, Ndikutinso amene wakanira kalikonse mu nsichi za Chisilamu wasanduka kafiri ndipo adzaphedwa ngakhale kuti wanena mau oti LAA ILAAHA ILLALLAH. Choncho onena mau oti: LAA ILAAHA ILLALLAH sakumuthandiza motani iye akakanira chilichonse mu nthambi za Chisilamu, ndiye zingamuthandize akakanira Tauheed yomwe ndi phata la chipembedzo cha Atumiki komanso mutu wake? Mwina mwake sunamve tanthauzo la Ma Hadith amenewa.

Tsopano mu nkhani ya Usaamat: Pakuti iye anapha munthu amene anadzitcha kuti ndi Msilamu chifukwa choti iye adaganiza kuti munthuyo sanangonena mau oti LAA ILAAHA ILLALLAH koma chifukwa choopa kukhetsedwa mwazi wake ndi kulandidwa chuma chake, ndipo munthu amene akuonetsera Chisilamu ndiwofunika kumusiya osam'patsa chilango china chilichonse mpaka chitaonekera kuchokera kwa iye chosemphana ndi Chisilamu. Allah akunena kuti: "*Eya, inu amene mwakhulupirira! Mukayenda pa njira ya Allah , musachite chinthu pokhapokha mutaonetsetsa bwino*" (Surat 4 :94). Choncho Ayat imeneyi ikusonyeza kuti munthu

ndiwofunika kumusiya ndikufufuza bwinobwino, choncho pambuyo pake chikaonekera chosemphana ndi Chisilamu aphedwe chifukwa cha mau Ake (SW) onena kuti "Choncho fufuzani" ndipo zikanakhala kuti saphedwa akanena mau oti LAA ILAAHA ILLALLAH ndiye kuti kufufuza kukanakhala kopanda phindu.

Chimodzimodzinso Hadith ina ija ikuti: tanthauzo lake ndi lija tanena lija, ndikutinso amene waonetsera Tauheed ndi Chisilamu ndiwofunika kumusiya, pokhapokha chitaonekera kwa iye chotsutsana ndi chikhulupiriro, ndipo umboni wa zimenezi ndi woti Mtumiki (SAW) ananena kuti : "*Kodi wamupha pambuyo poti wayankhula mau oti. 'LAA ILAAHA ILLALLAH'* **(Bukhaari).** Ananenanso kuti: "*Ndalamulidwa kuti ndilimbane ndi anthu kufikira atanena mau oti LAA ILAAHA ILLALLAH.*" (**Muslim)** ndi yemweyo amene adanena za makhawaarij kuti: "paliponse pomwe mukumane nawo muwaphe" chikhalirecho iwo anali anthu ochita ibaadat kwambiri komanso ochulukitsa kuyankhula mau oti LAA ILAAHA ILLALLAH, kufikira kuti Maswahaaba amadzipeputsa akaiona ibaadat ya anthu amenewo, ndipo iwo anaphunzira Ilm kuchokera kwa Maswahaaba, choncho LAA ILAAHA ILLALLAH, kuchuluka ibaadat kapena kudzitcha kuti ndi Msilamu sizinatchinjirize kuti asaphedwe kutaonekera kuchokera kwa iwo kusemphana ndi shariat.

**Abdun-nabiyy:** Unenapo chiyani pa zimene zinatsimikizika kuchokera kwa Mneneri (SAW): zoti anthu pa tsiku la Kiyaamat akapempha chipulumutso kudzera mwa Adam (AS) kenako mwa Nooh (AS) kenako mwa Ibrahim (AS) kenako mwa Mussa (AS) kenako mwa Issa (AS) , koma onsewo adzalandula kufikira kukathera kupempha chipulumutsoko kwa Muhammad (SAW). Zimenezi zikusonyeza kuti kupempha chipulumutso kudzera mwa wosakhala Allah si shirk.

**Abdullah:** Kumeneko ndiye kusokonezeka kochokera kwa iwe pa zoona zake za nkhaniyi, pakuti kupempha chipulumutsao kudzera mu cholengedwa cha moyo chomwe chilipo pa zimene chingathe, ife sitikutsutsa zimenezo, monga m'mene Allah wanenera kuti "*Choncho wakugulu lake uja adam'pempha chipulumutso pa mdani wake uja* **(Surat 28:15).** Monganso m'mene munthu adapempha chipulumutso kwa mnzake pa nkhondo ndi zina, mu zinthu zimene angazithe , ndipo ife tatsutsa ibaadat ya kupempha chipulumutso yomwe inu mumachita ku manda a ma Waliyy, kapena pomwe iwo kulibe mu zinthu zimene sangazithe wina koma Allah. Ndipo anthu adzakhala akupempha chipulumutso tsiku la Kiyaamat kudzera mwa aneneri, adzakhala akufuna kuchokera kwa iwo kuti am'pemphe Allah kuti awawerengere anthu ntchito zawo kuti anthu aku Jannat adzapume ku mazunzo pa bwalolo. Ndipo zimenezi ndizololedwa pa dziko lino la pansi komanso ku Aakhirat kuti umpitire munthu wochita zabwino akhale nawe ndikumva mau ako, ndipo nkumuuza kuti: "undipemphere zabwino kwa Allah", monga momwe ankachitira Maswahaaba a Mneneri (SAW) pomunfunsa iye ali moyo. Tsopano pambuyo pa kumwalira kwake (SAW) ndiye ayi ndithu iwo sanamufunse zimenezo pa manda ake, koma mashaikh oyambirira amudzudzula munthu amene wafuna kukam'pempha Allah pa manda ena alionse.

**Abdun-nabiyy:** Nanga unenapo chiyani pa nkhani ya Ibrahim (AS) ataponyedwa m'moto ndipo Jibril (AS) anamuonekera iye mu mlengalenga, ndipo anati "Kodi pali chimene ukufuna?" Ibrahim (AS) anati: 'Chofunikacho ngati chili chochokera

kwa iwe ndiye ayi'. Zikanakhala kuti kupempha chipulumutso kudzera mwa Jibril (AS) ndi shirk ndiye kuti Jibrilyo sakanamuuza Ibrahim (AS).

**Abdullah:** Kusokonezeka kumeneku ndi komwe kuja koyambirira kuja, ndipo Hadith yanenedwayo siyoona, ndipo titati tivomere kuti ndiyoona ndiye kuti Jibril (AS) anadzipereka kwa iye (AS) kuti amuthandize pa chinthu choti atha kuchichita pakuti za Iye (AS) ndi monga m'mene Allah wanenera kuti "*adam'phunzitsa wanyonga zambiri*" **(Surat 53:5)**. Choncho Allah akanamuloleza iye (AS) kuti achotse moto wa Ibrahim (AS) ndi za m'mbali za motowo kuchokera pansi ndi m'mapiri ndikukauponya kuvuma kapena ku zambwe sizikadam'kanika zimenezo.

Ndipo zimenezi zili ngati munthu wolemera wadzipereka kwa munthu wosauka kuti am'kongoze chuma kuti agwiritse ntchito pa zofuna zake ndipo munthu wosauka uja wakana ndikupirira kufikira pamene Allah adzampatsa rizq losakumbidwa ndi munthu wina. Nanga zimenezi zikugwirizana bwanji ndi ibaadat yopempha chipulumutso komanso shirk zomwe inu mukuchita panopa? Ndipo zindikira m'bale wanga kuti anthu oyambirira omwe anatumidwa bwana wathu Muhammad (SAW) kwa iwo, shirk yawo inali yopepuka kusiyana ndi ya anthu a **masiku athu ano chifukwa cha zinthu zitatu:**

**(i) Choyambirira:** Ndithu anthu oyambirira sanali kum'phatikiza Allah pa ibaadat ndi chinthu china koma pa mtendere pokha basi. Tsopano pa mavuto anali kumuyeretsera Allah chipembedzo, ndi umboni wa mau Ake (SW) onena kuti "*Ndipo akakwera m'chombo (ndikukumana ndi zoopsa) amam'pempha Allah modzipereka ndikumuyeretsera pempho. Koma akawapulumutsa ndikuwafikitsa kumtunda, iwo amayambanso kum'phatikiza Allah ndi mafano*" **(Surat 29:65)**. Ndinso mau Ake (SW) onena kuti: "*Ndipo mafunde onga thambo akawavindikira, amam'pempha Allah modzipereka ndikumuyeretsera pempho. Ndipo akawapulumutsira kumtunda, ena a iwo amachita zolungama. Sangawakane mau athu koma yense wa chinyengo wosathokoza*" **(Surat 31: 32)**. Ndipo mamushirk amene Mtumiki (SAW) anamenyana nao anali kum'pempha Allah ndi kupempha wosakhala Allah akakhala pa mtendere, koma akakhala pa mavuto sanali kupempha wina koma Allah yekha basi, ndipo anali kuyiwala mabwana awowo. Tsopano mamushirk a nthawi yathu ino ndithu amachipempha chosakhala Allah pa mtendere komanso pa mavuto. Ndipo mmodzi wa iwo akapanikizika amanena kuti: "Eya, iwe Mtumiki wa Allah, Eya, iwe Hussain" ndi ena otero. Koma ali kuti amene angamvetse zimenezo?

**(ii)** Chachiwiri, ndithu mamushirkna oyambirira anali kuwapempha pamodzi ndi Allah anthu amene ali pafupi ndi Allah (SW) Mwina anali Mneneri, kapena Waliyy, kapena mngero, kapena mocheperako mwala, kapena mtengo, ankamumvera Allah ndipo sanali kumunyoza. Koma anthu a masiku athu ano amam'pempha Allah pamodzi ndi anthu ena mwa anthu oipa kwambiri ndi amene amam'khulupirira kuti ndi wabwino ndi chimene sichimanyoza Allah monga mwala ndi mtengo, amaona kuti ndi chopepuka kuchipempha kuposa amene akumukhulupirira ndi kuona kupandukira kwake malamulo ndinso kuononga kwake pa dziko.

**(iii)** Chachitatu, ndithu mamushirkna onse a nthawi ya Mtumiki (SAW), shirk yao sidali mu umodzi wa uleri wa Allah, mosiyana ndi shirk ya anthu a m'mbuyo mwao, pakuti nthawi zambiri shirk imapezeka pa Uleri, monga imapezekeranso pa

umulungu. Pakuti iwo mwa chitsanzo amachiyika chilengedwe kuti ndicho chimalongosola zonse pa dziko lapansi monga kupereka moyo ndi kupereka imfa ndi zina zotero. Mwina ndimalize mau anga ponena nkhani yaikulu kuti umvetse zomwe zanenedwazo; nkhani yake ndiyakuti palibe kusiyana maganizo pa nkhani ya Tauheed kuti payenera kutsimikizira ndi mtima, kuyankhula ndi lirime ndi kugwira ntchito ndi ziwalo, choncho ngati chitasowa china chake mu zimenezi ndiye kuti munthuyo sangakhale Msilamu. Ndipo ngati atadziwa Tauheed ndipo sanaigwiritse ntchito ndiye kuti iyeyo ndi kafiri wamakani ngati Farao ndi Satana. Ndipo mu zimenezi anthu ambiri amalakwitsa, nkumanena kuti zimenezi ndizoona koma sitingathe kuzichita, ndipo sizikuloledwa kwa anthu a m'dziko lathu lino ndi ana a mtundu wathu, ndipo n'zofunika kugwirizana nawo ndi kuwanyengerera poopa zoipa zawo. Ndipo mphawi ameneyu sanazindikire kuti ambiri mwa atsogoleri a ukafiri amazindikira choonadi ndipo sanangochisiya choonadi koma kulandula kwina kwake , monga Allah wanenera kuti: "*Asinthanitsa Ayat za Allah ndi zinthu za dziko lapansi ndi mtengo wochepa, ndipo atsekereza anthu kunjira Yake. Ndithu, n'zoipa kwambiri zomwe iwo akhala akuchita*" **(Surat 9:9)** Ndipo amene wagwiritsa ntchito Tauheed pamwamba pokha (moyepula) asakuyimvetsetsa ndiponso asakuyikhululupirira ndi mtima wake ndiye kuti ameneyo ndi mchiphamaso, ndipo iye ndi woipitsitsa kwambiri kuposa kafiri weniweni, chifukwa cha Mau Ake (SW) onena kuti "*Ndithu achiphamaso adzakhala pansi penipeni pa moto*" **(Surat 4:145).** Ndipo ndi nkhani imeneyi zidziwika bwinobwino kwa iwe ukayilingalira m'malirime a anthu udzamuona amene akudziwa choonadi ndipo sakuchigwiritsira ntchito chifukwa cha kuopa kupunguka za dziko lake lapansi ngati Qaaroon, kapena ulemerero ngati Haamaan, kapena ufumu wake ngati Farao. Ndiponso umuona amene akugwiritsira ntchito pamwamba pokha mosachokera mumtima ngati achiphamaso, choncho ukamufunsa chomwe akukhulupirira ndi mtima wake udzaona kuti iye sakuchidziwa. Koma iwe uyenera kumvetsetsa ma Ayat awiri ochokera m'Buku la Allah (SW).

**i. Ayat yoyamba**: Iyi ndi yomwe yanenedwa kale, yomwe ndi mau Ake (SW) onena kuti "*Musapereke madandaulo (abodza) ndithu mwaonetsera ukafiri wanu poyera pambuyo pa kukhulupirira kwanu kwabodza*" **(Surat 9:66)**. Choncho ukazindikira kuti anthu ena amene anakathira nkhondo Rome limodzi ndi Mtumiki wa Allah (SAW) anasanduka makafiri chifukwa cha liwu lomwe adanena mosewera ndi mosereula uwona kuti amene akuyankhula liwu la ukafiri kapena kutsatira ukafiri poopera kupunguka chuma, kapena ulemerero, kapena kumusangalatsa wina wake, tchimo lake ndi lalikulu kwambiri kuposa amene akuyankhula liwu losereula nalo, chifukwa kawirikawiri munthu wosereula satsimikiza mu mtima mwake, chomwe amayankhula ndi lirime lake poseketsa anthu. Tsopano amene amayankhula mau a ukafiri kapena kugwiritsa ntchito ukafiriwo chifukwa cha mantha kapena kuzifunitsitsa zomwe zili kwa cholengedwa ndiye kuti wamuvomera Satana chiopsezo chake, Allah akunena kuti, "*Satana amakuopsezani ndi umphawi ndi kukulamulirani kuchita zoipa*" **(Surat 2:268)**, ndipo waopa chiopsezo chake; "*Ndithu uyu ndi Satana yemwe amaopseza abwenzi ake*" **(Surat 3: 175)**, ndipo sanam'vomere Wachifundo lonjezo Lake loti, "*Pomwe Allah akukulonjezani*

*chikhululuko ndi ubwino kuchokera kwa Iye*" **(Surat 2:268,)** ndipo sanaope chilango cha Allah, pakuti Iye akunena kuti, "*Choncho musawaope, ndiopeni Ine ngati inu mulidi okhulupirira*" **(Surat 3:175.)** Kodi munthu wotereyu ndiwoyenera kukhala mwa abwenzi a Wachifundo kapena mwa abwenzi a Satana?

**ii. Ayat yachiwiri**: Mau Ake (SW) onena kuti "*Amene akum'kana Allah pambuyo pomukhulupirira (chilango chachikulu chikumuyembekezera) kupatula yemwe wakakamizidwa, mtima wake utakhazikika pa chikhulupiriro; koma amene akutsanulira chifuwa chake kusakhulupirira, mkwiyo wa Allah uli pa iwo ndipo adzapeza chilango chachikulu*" **(Surat 16:106.)** Choncho Allah sadalandire kulandula kuchokera kwa amenewa kupatula kwa amene wakakamizidwa mtima wake uli wokhazikika pa chikhulupiriro. Tsopano wosakhala ameneyu ndithu wasanduka kafiri chimodzimodzi ngakhale atachita zimenezo chifukwa cha mantha, kapena kususukira chuma, kapena kum'kondweretsa wina wake kapena kuopa kupereka dziko lake, banja lake, mtundu wake, chuma chake kapena wachita zimenezo mosereula kapena pa chifukwa china chake, kupatula wokakamizidwa, pakuti Ayat ija ikusonyeza kuti munthu sakakamizidwa kupatula pa mau ndi zochita, koma chikhulupiriro cha mu mtima sangam'kakamize nacho aliyense, ndinso kuyankhula Kwake (SW) konena kuti: "*Zimenezo ndi chifukwa chakuti iwo adakonda kwambiri moyo wa dziko lapansi kuposa wa pa Tsiku Lomaliza ndikutinso Allah saongola anthu osakhulupirira*" **(Surat 16:107),** choncho wanenetsa kuti chilango sichinapezeke chifukwa cha chikhulupiriro, umbuli ndi kuipidwa ndi chipembedzo, kapena kuukonda ukafiri koma chifukwa chake ndichoti pakuchita zimenezo iye ali ndi gawo m'magawo a dziko lapansi motero wasankha zimenezi kusiya chipembedzo, ndipo Allah ndi amene akudziwa zoona zake. Ndipo pambuyo pa zonsezi Allah akuongole kodi sinakukwanire iweyo nthawi yoti ulape kwa Mbuye wako ndi kubwerera kwa Iye (SW) ndikutinso usiye zimene ukuchita pakuti zimene timakambazi monga wamvera sizamasanje nzoopsa kwambiri ndipo nkhaniyi ndi yaikulu komanso ndi mavuto akuluakulu.

**Abdun-nabiyy:** Ndikupempha chikhululuko kwa Allah ndiponso ndikuchita toba kwa Iye (SW), ndiponso ndikuikira umboni kuti palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma Allah ndikutinso Muhammad (SAW) ndi Mtumiki wa Allah, ndiponso ndithu ndachikana chilichonse chomwe ndinali kuchipembedza pambali pa Allah, ndikum'pemphanso Allah kuti andilandile madandaulo anga pa zomwe zinachitika kale, andikhululukire andichitire chili chonse mwa chifundo Chake, chikhululuko Chake ndi chisoni Chake, ndikutinso andilimbikitse pa Tauheed ndi pa chikhulupiriro changwiro kufikira ndidzakumane Naye. Ndikum'pemphanso kuti akulipire zabwino iwe m'bale wanga Abdullah chifukwa cha malangizowa pakuti Deen ndikulangizana, komanso chifukwa cha kudzudzula kwako pa zimene ine ndikuchita; ndipo limenelo ndi dzina langa loti Abdun-nabiyy, ndipo ndikukuuza kuti ine ndalisintha dzinalo kuti tsopano ndine AbdulRahmaan, komanso chifukwa chakudzudzula choipa cham'katikati chomwe ine ndinali nacho, chomwe ndi chikhulupiriro chosokera choti ndikanakakumana ndi Allah ndili ndi chikhulupiriro chimenecho sindikadakapambana ngakhale pang'ono. Koma ndikufuna ndipemphe pempho lomaliza kuchokera kwa iwe loti undiuze ine zoipa zina zomwe anthu ambiri amalakwitsa mu zimenezo.

**Abdullah:** Palibe vuto;  ndibwereke makutu ako.

- Upewe kukhala mu zinthu zomwe mkati mwake muli kusiyana maganizo kuchokera mu Quràn ndi Sunnat kutsatira zomwe zili ndi mkangano mkati mwake pofunafuna chisokonezo ndi kufunafuna tanthauzo lake, koma zoona zake n'zakuti palibe amene amadziwa tanthauzo lake koma Allah, ndipo chisonyezo chako chikhale cha anthu ozama m'maphunziro a Shariat, amene amayankhula pa za ndime zokuluwika kuti "Tawakhulupirira ma Ayat onse kuti ndi ochokera kwa Mbuye wathu,"

Ndipo zinthu zimene anthu akusiyana maganizo, Mtumiki (SAW) anati "*Chisiye chomwe chikukukaikitsa ndikuchita chomwe sichikukukaikitsa*" **(Ahmad, Tirmidhi)**. Mneneri (SAW) anatinso "*Choncho amene angapewe zokuluwika ndiye kuti wadziyeretsa ku Deen yake ndi ulemu wake ndipo amene wagwera mu zokaikitsa adzagwera mu Haraam*" **(Bukhaari, Muslim)** . Mneneri (SAW) anatinso "Tchimo *ndi chomwe chimagundagunda m'chifuwa mwako ndipo umaipidwa kuti anthu achitulukire*." **(Muslim)**. Anatinso Mneneri (SAW) kuti: "*Ufunse mtima wako ndi moyo wako - ananena zimenezo katatu - ubwino ndi chinthu chomwe moyo wakhazikika pa chimenecho, ndipo tchimo ndi chinthu chomwe chikugundagunda m'moyo ndikumakaikakaika m'chifuwa ngakhale anthu atakuuza kambirimbiri. Inenso ndikukuuza*." **Ahmad.**

- Upewe kutsatira zilakolako pakuti Allah wachenjeza zimenezo ndi mau Ake onena kuti "*Kodi wamuona yemwe wachichita chilakolako chake kukhala mulungu wake*" **(Surat 25:43)**
- Upewe kukhala ndi mbali powatsatira atsogoleri, maganizo ndi chomwe makolo ankachita, pakuti kutero kumatsekereza pakati pa munthu ndi choonadi, ndithu choonadi ndi chotaika cha munthu wokhulupirira paliponse angachipeze ndiye kuti iye ndi woyenerera chimenecho, Allah akunena kuti: "*Ndipo kukanenedwa kwa iwo kuti 'Tsatirani zimene Allah wavumbulutsa'* ", akunenanso "*Koma tikutsata zimene tidawapeza nazo atate athu;" kodi ngakhale kuti atate awo sadali kuzindikira chilichonse ndiponso ngakhale sadali oongoka (awatsatirabe)?* **(Surat 2:170)**
- Upewe kudzifananizira ndi makafiri, pakuti kutero ndiye chiyambi cha tsoka lililonse, Mtumiki (SAW) anati "*Munthu amene angadzifananitse ndi anthu ena ndiye kuti iye ndi mmodzi wa iwo*" **(Abu Dawood).**
- Upewe kuyedzamira pa chinthu chosakhala Allah, pakuti Allah wanena kuti "*Ndipo amene akutsamira kwa Allah ndiye kuti Allah ali Wokwana kwa iye*" **(Sura 45:3)**
- Usachimvere cholengedwa chilichonse pa zomunyoza Allah. Mtumiki (SAW) anati  "Palibe zochimvera cholengedwa pa zomunyoza Mlengi (SW)".
- Upewe kumuganizira Allah zoipa, pakuti Iye (SW) ananena mu Hadith Qud - si kuti "*Ine ndimakhala pafupi ndi maganizo a kapolo wanga pamene akuganiza za ine."* **(Bukhaari, Muslim)**
- Upewe kuvala chibangiri kapena ulusi ndi zina zonga zimenezo ndicholinga chotchinjiriza matsoka asanagwe kapena kuchotsa matsokawo akagwa.
- Upewe kudzipachika zithumwa pofuna kudzitchinjiriza ku diso la upandu, pakuti kutero ndi shirik, Mtumiki (SAW) ananena kuti "*Munthu amene wadzipachika chinthu amasiyidwa ku chimenecho kuti chimuthandize*" **(Tirmidhi)**
- Upewe kufunafuna madalitso kudzera m'miyala, mitengo,zinthu za make dzana ndi zomangamanga, pakuti kutero ndi shirk.

- Upewe kuombeza mwayi ndi tsoka kuchokera ku china chake, pakuti kutero ndi shirk Mtumiki (SAW) ananena katatu kuti: "*Kuombedza ndi mbalame ndi shirk*" **(Abu Dawood.)**
- Upewe kuwavomereza anthu a matsenga ndi ochita maula kudzera mu nyenyezi omwe amadzitama kuti amadziwa za mseri, ndipo amaonetsa nyenyezi m'mabuku, komanso mwayi kapena tsoka kwa eni nyenyezizo, ndipo kuwavomereza pa zimenezo ndi shirk, chifukwa choti palibe amene amadziwa za mseri kupatula Allah.
- Upewe kunena kuti mvula imagwa chifukwa cha nyenyezi kapena nyengo, pakuti kutero ndi shirk, koma ziperekedwe kwa Allah (kuti ndi Amene amagwetsa mvula).
- Upewe kuchilumbira chosakhala Allah, cholumbiridwacho ngakhale chitaopsa motani pakuti kutero ndi shirk, ndipo ndithu mu Hadith ya Mtumiki (SAW) mwadza mau onena kuti "*Amene wachilumbira chosakhala Allah ndithu wachita ukafiri kapena wachita shirk*" **(Ahmad)** monga kumulumbira Mneneri, kapena Amaanat, kapena ulemerero, kapena chitetezo kapenanso moyo.
- Upewe kuisambula nyengo, mphepo, kapena dzuwa kapena kuzizira, kapenanso kutentha, pakuti kutero kudzakhala kumusambula Allah Amene anazilenga zimenezo.
- Upewe liwu lonena kuti "zikanakhala mwakuti" akakupeza mavuto, pakuti liwuli limatsegula ntchito ya Satana, ndiponso mu liwu limeneli muli kudzudzula chikonzero cha Allah, koma unene kuti ndi chikonzero cha Allah ndipo wachita zomwe wafuna.
- Upewe kuwachita manda kukhala malo opempherera, chifukwa choti mu Mzikiti momwe muli manda simuloledwa kuswaliramo. Ndipo nkhani yachokera kwa Aishat (RA) iye anati: "Ndithu Mtumiki (SAW) ali mu ululu wa imfa anati: '*Allah anatemberera Ayuda ndi Akhristu, iwo anawachita manda a Aneneri awo kukhala malo opempherera, Allah akuchenjeza pa zomwe amachita iwo*." Bibi Aishat (RA) anati: "*Pakadapanda zimenezo Maswahaaba akanawatukula manda ake (SAW).*" **(Bukhar).** Ananenanso Mtumiki (SAW) kuti: *Ndithu amene analipo inu musanadze anali kuwachita manda a Aneneri awo ndi a omwe anali ochita zabwino mwa iwo kukhala malo opempherera, choncho musawachite manda kukhala malo opempherera pakuti ine ndithu ndikukuletsani zimenezo*" **(Abu Uwaanah.)**
- Upewe kuvomereza maHadith omwe anthu abodza amam'namizira Mtumiki (SAW) olimbikitsa kupempha kudzera mwa uchenicheni wa iye (SAW) kapena mwa anthu ochita zabwino ochokera mu Ummat wake (SAW) ndipo maHadith amenewo ndi opekedwa onamiziridwa kwa iye (SAW); ndipo ena mwa iwo ndi awa: "Pemphani kudzera mu ulemerero wanga, pakuti ulemerero wanga pamaso pa Allah ndi wolemekezeka kwambiri". Inanso: "zikakuvutani zinthu muyenera kupita kwa anthu a m'manda". Inanso: "ndithu Allah amamuika mngero pa manda a Waliyy aliyense yemwe amakwaniritsa zofuna za anthu". Inanso: "ngati mmodzi wa inu atakhala ndi maganizo abwino ndi mwala, utha kumuthandiza", ndi maHadith ena ambiri.
- Upewe kuchita zikondwerero zomwe zimatchedwa kuti ndi za chipembedzo, monga chikondwerero cha kubadwa kwa Mneneri (SAW), cha Israai ndi Miiraaj ndi zina zotero pakuti izo ndi zopeka palibe umboni wake wochokera kwa Mtumiki (SAW) kapena kwa Maswahaaba ake amene anali kum'konda Mtumiki (SAW) kuposa ife, komanso omwe anali akufunitsitsa zabwino kuposa ife, zikanakhala zimenezo kuti ndi zabwino ndiye kuti akadatitsogolera ife ku zimenezo.

# UMBONI WONENA KUTI PALIBE WOPEMBEDZEDWA MWA CHOONADI KOMA ALLAH

**Liwu** limeneli lasonkhanitsa nsichi ziwiri. **Yoyamba:** **(Palibe wopembedzedwa)** komwe ndikutsutsa umulungu wachoonadi kwa wina aliyense wosakhala Allah. **Yachiwiri:** **(koma Allah)** kumeneko ndikutsimikizira za umulungu weniweni kwa Allah yekha. Adanena Allah (SW) kuti: "*Kumbukira pamene Ibrahim adanena kwa bambo ake ndi anthu ake: 'Ndithudi ine ndadzitalikitsa ku zomwe mukupembedza. Kupatula Amene adandilenga ndipo andiongolera*". Choncho ibaadat yomuchitira Allah siingakwanire pokhapokha payenera kuti ikhale yomuchitira Iye yekhayo. Ndipo umodzi wa Allah siungavomerezeke pokhapokha posonkhanitsa pakati pomuchita Allah kuti ndi wa mmodzi wake ndi kudzitalikitsa ku shirk ndi anthu ake.

Zinalandiridwa kuchokera mu Athar kuti kiyi yotsegulira Jannat ndi mau oti: (LAA ILAAHA ILLALLAH), koma kodi aliyense amene wanena mauwa ndi woyenera kuti Jannat ikatsegulidwe kwa iye? Wahab bin Munabbih (RA) anafunsidwa kuti: "**Kodi mau oti LAA ILAAHA ILLALLAH Sali kiyi ya ku Jannat?"** Iye poyankha anati ndi momwemodi, koma kuti palibe kiyi ina iliyense koma iyenera kukhala ndi mano, choncho ukabweretsa kiyi yokhala ndi mano chitseko chidzatsegulidwa kwa iwe, koma ngati ilibe mano chitseko sichingakutsegukire.

Ndipo adza kuchokera kwa Mneneri wathu (SAW) maHadith ambiri onsewo akulongosola mano a kiyi imeneyi; monga mau ake (SAW) onena kuti: "Amene wanena LAA ILAAHA ILLALLAH moyeretsa mtima, 'motsimikizira ndi mtima wake' (akuwanena mauwo m'choonadi kuchokera mu mtima mwake" ndi ena otero, pakuti maHadith amenewa ndi ena akukulumikiza kulowa ku Jannat ndi kuzindikira tanthauzo la LAA ILAAHA ILLALLAH ndi kukhazikika pa mauwo mpaka kumwalira ndi kudzichepetsa ku zofuna za mauwo ndi zina zotero.

Ndipo kuchokera m'maumboni ambiri maUlama atulutsamo zofunikira zomwe zili zofunika kuzikwaniritsa ndi kuchotsa zoletsa kuti liwu loti LAA ILAAHA ILLALLAH likhale kiyi yokatsegulira Jannat ndipo limpindulire wonena liwuli. Ndipo zofunikira zimenezi ndiye mano a kiyi omwe ndi izi:-

❶ **Kuzindikira:** Pakuti liwu lililonse lili ndi tanthauzo, choncho n'zofunika kuti udziwe tanthauzo la mau oti LAA ILAAHA ILLALLAH kuzindikira kuchotsa umbuli, choncho liwuli likuletsa umulungu kwa amene sali Allah ndipo likutsimikizira umulunguwo kwa Iye (SW), kutanthauza kuti palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma Allah. Allah akunena kuti "*Kupatula amene akuyikira umboni choonachi pomwe iwo akuchidziwa bwino*" **(Surat 43:86,)** Mtumiki (SAW) nayenso ananena kuti: "*Amene wamwalira akuzindikira kuti palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma Allah akalowa ku Jannat*". **(Muslim.)**

❷ **Kutsimikiza:** Komwe ndikuti utsimikize kwenikweni cholinga cha mauwo, pakuti mauwo salandira kukaika, kapena kuganizira, kapena kudodoma kapena kukaikira koma zifunika kuti ukhale ndi chitsimikizo chenicheni ndithu. Allah (SW) wanena posimba za okhulupirira kuti: "Ndithu, amene ali okhulupirira moona

ndi omwe akhulupirira mwa Allah ndi Mtumiki Wake, ndipo kenako sadakaike, n'kuchita nkhondo pa njira ya Allah, ndi chuma chawo ndi matupi awo,iwowo ndiwo oona pa chikhulupiriro chawo." (Surat 49:15,). Choncho sizikukwanira kungowayankhula kokha mauwa koma zikufunika kuti mtima utsimikize. Motero ngati sikunapezeke kutsimikiza kwa mtima ndiye kuti umenewo ndi uchiphamaso weniweni. Mtumiki (SAW) anati "*Ndikuikira umboni kuti palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma Allah ndikuti ine ndi Mtumiki wa Allah, munthu sakakumana ndi Allah atatenga mau awiriwa asakuwakaikira koma akalowa ku Jannat*". **( Muslim.)**

**❸ Kuvomera:** Choncho ukazindikira ndi kutsimikiza ndiye kuti kuzindikira kotsimikizaku kuyenera kuti kukhale ndi zotsatira zake ndipo zimenezo zingachitike povomera zomwe liwuli lafuna ndi mtima komanso lirime. Choncho amene wakana ulaliki wa Tauheed ndipo sanauvomere ameneyo ndi kafiri chimodzimodzi ngati kukanako kunachitika chifukwa cha kudzikweza, kapena makani, kapenanso kaduka. Ndithu Allah wanena za makafiri amene anakana ulaliki wa Tauheed chifukwa cha kudzikweza kuti: "*Ndithu iwo ankati akauzidwa kuti palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma Allah ankadzitukumula*". **(Surat 37:35.)**

**❹ Kugonjera:** Tauheed imafuna kugonjera mokwanira, ndipo amenewo ndiwo mayeso enieni, komanso ntchito zoonekera pa chikhulupiriro, ndipo zimenezo zitha kutheka potsatira zomwe Allah analamula ndi kusiya zomwe anaziletsa, monga Allah wanena kuti "*Ndipo amene akupereka nkhope yake kwa Allah ali wochita zabwino, ndiye kuti wagwiritsa chigwiriro cholimba .Ndipo mapeto a zinthu zonse nkwa Allah basi*" **(Surat 31: 22,)** ndipo kumeneku ndiko kukwaniritsa kwa kugonjera.

**❺ Kuyankhula** zoona: Mu mauwo uku ukukana bodza, pakuti amene wanena mauwo ndi lirime lokha basi mtima wake ukukanira ndiye kuti ameneyo ndi mchiphamaso, ndipo umboni wake ndi mau Ake (SW) pakudzudzula kwake kowadzudzula achiphamaso: "*Akunena ndi malirime awo zomwe m'mitima mwao mulibe*" **(Surat 48:11.)**

**❻ Chikondi:** Choncho wokhulupirira alikonde liwuli, ndipo akonde kutsatira zofuna zake za liwulo, ndipo awakonde eni liwuli amene akutsatira mauwo. Ndipo chizindikiro cha chikondi cha munthu kwa Mbuye wake ndiko kutsogoza zomwe Allah amazikonda ngakhale zitasemphana ndi zofuna zake, ndi kupalana ubwenzi ndi amene Allah ndi Mtumiki Wake apalana nao ubwenzi ndinso kuchita naye udani amene Allah wachita naye udani komanso kumutsatira Mtumiki wake ndi kutsatira mapazi ake (SAW) komanso kuvomera chiwongoko chake (SAW).

**❼ Kuyeretsa mtima:** Poyankhula mauwo pasakhale kufuna china chake koma nkhope ya Allah (SW), Allah akunena kuti: "*sanalamulidwe china koma kuti am'pembedze Allah momuyeretsera chipembedzo popendekera ku choona*" **(Surat 98: 5)** Nayenso Mtumiki (SAW) anati: "*Ndithu Allah wauchita moto Haraam kukamuotcha amene wanena mau oti LAA ILAAHA ILLALLAH akufunitsitsa (ndi mau amenewo) nkhope ya Allah*". **(Bukhaari).**

# UMBONI WONENA KUTI MUHAMMAD NDI MTUMIKI WA ALLAH

Maliro akaikidwa m'manda amayesedwa ndi kufunsidwa mafunso atatu, akayankha mafunso atatuwo ndiye kuti wapulumuka, ndipo ngati sanawayankhe molondola ndiye kuti waonongeka, ndipo mafunso ake ena ndi awa: Mneneri wako ndi ndani? Funso limeneli sangayankhe kupatula yekhayo amene Allah anam'patsa kuthekera kokwaniritsa zofunikira zake pa dziko lapansi ndipo adzamulimbikitsa ndi kumuuza iye ali m'manda ake, tero likam'pindulira kumapeto ake pa tsiku losapindula chuma kapena ana. Ndipo zofunikirazo ndi izi:

❶ **Kumumvera Mneneri (SAW) zimene analamula:** Pakuti Allah (SW) anatilamula kumumvera iye (SAW) motero anati, "*Amene angamumvere Mtumiki ndiye kuti wamvera Allah*" **(Surat 4:80).** Wanenanso kuti Nena "*Ngati mukum'konda Allah nditsatireni ine Allah akukondani*" **(Surat 3:31.)** Ndipo kulowa kokha ku Jannat kukugwirizana ndi kumumvera kokhako, pakuti Mtumiki (SAW) anati "Anthu onse a ummat wanga akalowa ku Jannat kupatula amene wakana, maswahaaba (RA) anati: "*Eya, iwe Mtumiki wa Allah! Ndi ndani akukana?" Mtumiki (SAW) anati, "Amene wandimvera ine akalowa ku Jannat ndipo amene sanamvere ine ndiye kuti ndithu wakana*" **(Bukhaari)** .Ndipo amene amam'konda Mneneri (SAW) ndiye kuti ayenera kumumvera popeza kumvera ndi chipatso cha chikondi komanso ndi chisonyezo cha ntchito pa chikondi.

❷ **Kumuvomera pa zimene wanena:** Choncho amene watsutsa chinthu chotsimikizika kuti ndi choona kuchokera kwa Mneneri (SAW) chifukwa cha chilakolako ndi zofuna zake ndiye kuti wamutsutsa Allah ndi Mtumiki Wake, chifukwa Mneneri (SAW) ndi wotetezedwa ku tchimo ndi bodza, Allah akunena kuti: "*Ndipo sayankhula zofuna za mtima wake*" **(Surat 53:3).**

❸ **Kupewa zomwe analetsa:** moyambirira ndi tchimo lalikulu mwa machimo onse lomwe ndi shirk komanso mowadutsa machimo aakuluakulu komanso oononga, ndi kumalizira kusiya machimo aang'onoang'ono komanso zinthu za makrooh, ndiponso momwe chingakhalire chikondi cha Msilamu kwa Mneneri wake (SAW), chikhulupiriro chake chimaonjezereka, ndipo chikhulupiriro chake chikaonjezereka, Allah amam'pangitsa iye kuikonda ntchito yabwino, komanso amam'pangitsa iye kuipidwa ndi ukafiri, kupandukira malamulo ndi kunyozera malamulo.

❹ **Asapembedzedwe Allah koma m'njira yomwe Allah analamula kudzera pa lirime la Mneneri wathu (SAW):** Choncho maziko enieni mu ibaadat ndiko kusiya njira zoletsedwa, motero sizikuloledwa kuti Allah apembedzedwe m'mapembedzedwe ena alionse koma m'mapembedzedwe omwe anadza kuchokera kwa Mtumiki (SAW). Mtumiki (SAW) anati "*Amene wachita chinthu chomwe ife sitinalamule ndiye kuti chidzabwezedwa kwa iye mwini*". **(Muslim)**

**<u>PHINDU</u>:**

Zindikira kuti zili waajib kum'konda Mneneri (SAW) ndi zomwe iye adabweretsa. Amene angade kalikonse mu zinthu zimene iye adabweretsa angakhale atazigwiritsa ntchito iye ndi zimenezo ndi kafir chabe koma ndi wofunika kuti

akhale wokondedwa kwambiri kwa iwe kuposa chilichonse komanso kuposa moyo wako, pakuti amene wachikonda chinthu amachitsogoza pa chilichonse ndi kusankha kugwirizana nacho m'machitidwe. Choncho woona mtima pakum'konda Mtumiki (SAW) ndi amene chimaonekera pa iye chizindikiro cha kum'konda pomumvera iye ndi kutsatira sunnat yake (SAW) m'mayankhulidwe ndi m'machitidwe ndi kumvera malamulo ake komanso kupewa zomwe analetsa ndikutsatira miyambo yake pa mavuto ndi pa mtendere, pa chisangalalo komanso pa mavuto,pakuti kumvera ndi kutsatira ndizo zipatso za chikondi, ndipo popanda ziwirizi ndiye kuti chikondicho ndi chabodza..

**Kumkonda Mnenenri (SAW) kuli ndi zizindikiro zambiri ndipo zina mwa izo ndi izi:-**

**i.** Kuchulutsa kumutchula ndi kumufunira zabwino pakuti amene wachikonda chinthu amachitchulatchula.

**ii.** Kukhumbira zokakumana naye, pakuti bwenzi aliyense amakhumba za kukumana ndi bwenzi Lake.

**iii.** Kumukuza ndi kumulemekeza pomutchula, Ishaq (RA) anati Mtumiki (SAW) atamwalira: "Maswahaaba a Mneneri (SAW) sanali kumutchula iye (SAW) koma anali kudzichepetsa ndi kugwidwa tsembwe makungu awo komanso anali kulira.

**iv.** Kudana naye amene akudana ndi iye (SAW) ndi kuchita naye chidani amene akuchita chidani ndi iye (SAW) komanso kum'pewa amene wasiya Sunnat yake (SAW) nabweretsa zopeka mu Deen yake mwa eni ma Bidah ndi achiphamaso.

**v.** Kum'konda amene Mtumiki (SAW) anam'konda, kuyambira anthu a m'nyumba mwake, akazi ake ndi Maswahaaba ake ochokera ku Makkat ndi ku Madinat , ndikudana nawo amene akudana ndi iwo kapena kuwatukwana.

**vi.** Kutsatira makhalidwe ake (SAW) olemekezeka, pakuti iye (SAW) anali ndi makhalidwe abwino kwambiri kuposa anthu onse kufikira Bibi Aishat (RA) ananena kuti makhalidwe a Mtumiki (SAW) anali Quran (anadzikakamiza kuti sangachite chinthu koma chomwe Quràn yalamula).

Tsopano mbiri za Mneneri (SAW) ndithu anali wolimba mtima kuposa anthu onse, ndipo anali wolimba mtima kwenikweni nkhondo zikafika pachiyindeyinde, woolowa manja kuposa ena onse kwenikweni m'mwezi wa Ramadhan, wopereka malangizo kwambiri kwa anthu, woleza mtima kuposa anthu onse, sanaperekepo chilango pofuna kudzibwezerera, anali woopsa kwambiri kuposa aliyense pa chilamulo cha Allah , wodzichepetsa kwambiri modzilemekeza kuposa anthu onse, wamanyazi kwambiri kuposa buthu limene lili m'nyumba mwake, wabwino kuposa anthu onse kwa anthu a m'nyumba mwake, wachisoni kwambiri ndi zolengedwa kuposa zolengedwa zonse ndi zina zambiri.

# TWAHARAH

Swalaat ndi nsichi yachiwiri mu nsichi za Chisilamu, ndipo singatheke koma ndi Twaharah, komanso Twaharah singachitike koma ndi madzi kapena dothi.

**MITUNDU YA MADZI: 1.** Madzi a TWAHIR: Amenewo ndi madzi omwe ali oyera pa iwo okha omwe angathe kuyeretsa chinthu china, ndipo madzi amenewo amachotsa hadath ndi najisi. **2.** Madzi a Najisi: Amenewo ndi madzi omwe akumana ndi Najisi ngati madziwo ali wochepa , kapena makomedwe ake asintha, kapena mtundu wake , kapena fungo lake chifukwa cha Najisi ngati madziwo anali ochuluka.

**CHENJEZO:** Madzi ochuluka sakhala a najisi pokhapokha ngati najisi itasintha imodzi mwa mbiri za madziwo zomwe ndi mtundu wake, kapena makomedwe ake, kapena fungo lake. Ndipo madzi ochepa amakhala a Najisi chifukwa chokumana ndi Najisi, ndipo madzi amatchedwa kuti ndi ambiri ngati atapitirira pa mlingo wa makullat awiri omwe ndi madzi okwanira pafupifupi malita (210).

**ZIWIYA:** Chiwiya chilichonse cha Twahir chikuloledwa kukhala nacho kuchigwiritsira ntchito kupatula chiwiya chopangidwa ndi golide kapena siliva, ndipo Twaharah ikhoza kutheka pogwiritsa ntchito chiwiya cha golide kapena siliva koma ndi tchimo. Komanso ziwiya ndi nsalu za makafiri zikuloledwa kugwiritsa ntchito pokhapokha titazindikira kuti zili ndi Najisi.

**CHIKOPA CHA CHIBUDU:** Mosashashalika ndi najisi basi. Chibudu chikhoza kukhala chimodzi mwa mitundu iwiri iyi:- **1.** Chikhalire nyama yake sidyedwa. **2.** Nyama yake imadyedwa koma sinazingidwe ndipo chibudu chomwe nyama yake imadibwa chimene sichinazingidwe chikanyulidwa chikopa chake chikuloledwa kuchigwiritsira ntchito mu zinthu zouma osati zaziwisi..

**ISTINJAA:** Kumeneko ndiye kuchotsa nyasi yomwe yatuluka kuchokera kumaliseche akutsogolo ndi kumbuyo, choncho kuchotsako kukakhala kuti kwachitika ndi madzi kumatchedwa kuti Istinjaa, koma ngati kwachitika ndi mwala kapena tsamba ndi zofanana ndi ziwirizi kumatchedwa kuti istijmaar .Ngati munthu akugwiritsa ntchito kuseta kokha n'zofunikira kuti choseteracho chikhale cha Twahir, chololedwa kusetera, choyeretsa chosadibwa , ndipo kusetako kukhale ndi miyala itatu kapena kuchulukirapo. Ndipo kuchita Istinjaa kapena kuseta n'kofunika pa chilichonse chotuluka kuchokera ku maliseche awiri.

Zili haraam kwa amene akudzithandiza kukhala pa malo wodzithandizirawo nthawi yaitali kuposa yofunikira, kuchita chimbudzi kapena kukodza pomwe anthu amamwerapo madzi, kapena m’njira yomwe amadutsa anthu kapena pansi pa mthunzi womwe uli ndi phindu kapena pansi pa mtengo womwe uli ndi zipatso ndi kulunjika ku Qiblat ngati ali pamtetete.

Ndipo zili makrooh kwa amene akudzithandiza kulowa m’chimbudzi atanyamula chinthu chomwe chatchulidwa mkati mwake Allah, kuyankhula pa nthawi yodzithandiza, kukodzera pa una ndi pamalo ponga una. Kugwira maliseche ndi dzanja lake lamanja, kulunjika ku Qiblat ngati sali mu chomangidwa, ndipo zanenedwazi zikuloledwa ngati pali chifukwa. Ndipo zili sunnat kwa amene akudzithandiza kusiyanitsa chiwerengero cha istinjaau (kutawasa) kapena kuseta ndi kuphatikiza pogwiritsa ntchito mwala ndi madzi.

**MISWAAK:** Zili Sunnat kutsuka mano ndi kamtengo kofewa ngati kamtengo ka msawu, ndipo kudzafunika kwambiri kutsuka manoko pofuna kuswali, kuwerenga Qur'an, ndi pofuna kuyamba wudhu asanachukuche mkamwa, akangodzuka kuchokera kutulo, polowa mu mzikiti ndi m'nyumba, likasintha fungo la mkamwa ndi fungo la china chake. Ndipo ndi sunnat potsuka mano ndi kuchita twahaarat kuyambirira ku manja, komanso ndi Sunnat kugwiritsa ntchito dzanja la manzere pochotsa zinthu zosakhala zabwino.

**WUDHU NDI NSICHI ZAKE: Nsichi zake ndi izi: 1)** Kusambitsa nkhope, ndipo mukusambitsa nkhopemo muli kuchukucha mkamwa ndi kutsuka m'mphuno. **2)** Kusambitsa manja awiri kuchokera mu nsonga za zala mpaka mu akasukusuku awiri. **3)** Kupaka madzi mutu wonse pamodzi ndi makutu awiri. **4)** Kusambitsa mapazi awiri pamodzi ndi misomali. **5)** Kusambitsa mwa ndondomeko. **6)** Kufulumira.

**ZOFUNIKA ZAKE:** Kunena Bismillah asanayambe wudhu, kusamba m'manja kwa amene wangodzuka kuchokera mtulo ta usiku katatu asanalowetse manjawo m'madzi.

**MASUNNAT A WUDHU:** Kuchita miswaak, poyambirira kusambitsa zikhato ziwiri, kutsogoza kuchukucha mkamwa ndi kutsuka m'mphuno asanasambitse nkhope, kufikitsa madzi kum'mero pochukucha ndi kufikitsa madzi m'mphuno kwa amene sali pa swaum, kutsanula ndevu zambiri, kutsanula zala potsuka ziwalo kuyambira kumanja, kutsuka ziwalo kachiwiri ndi kachitatu, kuthira madzi m'mphuno ndi dzanja la manja ndi kuwamina ndi dzanja la manzere, kunyula ziwalo zopangidwa wudhu, kukwaniritsa wudhu bwinobwino ndi kuchita Du'aa pambuyo pake yomwe inadza kuchokera kwa Mtumiki (SAW).

**ZOMWE ZILI MAKROOH PA WUDHU:** Kuchita wudhu ndi madzi ozizira kwambiri kapena otentha kwambiri, kuonjezera pa katatu posambitsa chiwalo chimodzi, kukuntha madzi kuchokera mu ziwalo, kutsuka mkati mwa diso, tsopano kupukuta ziwalo pambuyo pa wudhu n'kololedwa.

**CHENJEZO:** Pochapa mkamwa pafunika kuwachukucha madzi mkamwamo, ndipo potsuka m'mphuno pafunika kulowetsa madzi m'mphuno pogwiritsa ntchito mpweya osati ndi dzanja lokha ayi chimodzimodzinso kugwiritsa ntchito mpweya powamina , ndipo ziwirizi sizingatheke pokhapokha mkachitidwe kameneka.

**KACHITIDWE KA WUDHU:** Kachitidwe ka wudhu ndi aka: Atsimikize mu mtima kenako anene Bismillah ndikusamba m'manja kenako achukuche mkamwa ndi kutsuka m'mphuno kenako asambitse nkhope yake; ndipo malire a nkhope kuchokera moyambira kumera tsitsi la m'mutu lomera mwa chizolowezi mpaka ku chibwano m'menemo mulitali, ndipo kuchokera kukhutu mpaka khutu lina m'menemo mulifupi, kenako asambitse manja ake awiri pamodzi ndi mikono yake iwiri ndinso akasukusuku ake awiri. Kenako apake madzi pamwamba pa mutu wake wonse kuchokera m'malire mwa nkhope mpaka ku nkhongo yake, ndipo mopanda tsitsi kuseli kwa makutu ndi mbali ya mutu, ndipo alowetse zala zake ziwiri za mkomba phala m'mabowo a makutu ake awiri ndikupaka madzi ndi zala zake ziwiri zazikuluzikulu kunja kwa makutuwo kenako nkusambitsa mapazi ake awiri pamodzi ndi misomali.

**CHIDZIWITSO:** Ndevu zikakhala zosathinana padzafunika kusambitsa chikopa chomwe chili pansi pa ndevu, koma zikakhala zothinana adzasambitsa pamwamba pake.

**KUPAKA MADZI PAMWAMBA PA KHUF ZIWIRI:** Khuf ndi chovala cha phazi chopangidwa kuchokera ku chikopa ndi zina zotero, choncho chikakhala chopangidwa kuchokera ku *wool* ndi chofanana ndi *wool* (monga thonje ndi zina) chimatchedwa sokosi. Ndipo kupaka madzi pamwamba pa makhuf awiri nkololedwa ngati ali pa Hadath yaing'ono yokha.

**KUPAKA MADZI PA KHUF KULI KOLOLEDWA NGATI PALI ZOFUNIKIRA ZINGAPO IZI: 1)** Khuf ziwirizo zivalidwe ali ndi Twaharat yokwanira atasambitsa mwendo wake wachiwiri. **2)** Wudhuwo upangidwe ndi madzi. **3)** Khuf'zo zibise malo omwe ali Fardh kuwasambitsa. **4)** Zikhale zololedwa kuzivala. **5)** Khuf zenizenizo zikhale za Twaharat

**NDUWIRA:** Zikuloledwa kupaka madzi pamwamba pa nduwira ngati pali zofunikira zingapo: **1)** Nduwirayo ikhale ya munthu wamwamuna. **2)** Ikhale yobisa m'mutu mwachizolowezi. **3)** Kupakako kukhale chifukwa cha Hadath yaing'ono. **4)** Twaharat yo ikhale yogwiritsira ntchito madzi.

**MPANGO:** Ndipo pamwamba pa mpango pakuloledwa kupaka madzi ngati pali zofunikira zingapo: Mpangowo ukhale wa munthu wamkazi. **1)** Ukulungidwe mpangowo pansi pa khosi. **2)** Kupakako kukhale chifukwa cha kuonongeka wudhu. **3)** Twaharat yo ikhale yochita ndi madzi. **4)** Mpangowo ubise malo a chizolowezi m'mutu.

**KUTALIKA KWA NTHAWI YOCHITIRA MAS – H:** Kwa munthu amene sali pa ulendo atha kupaka mu nthawi yokwanira usiku ndi usana pa ma ola 24, ndipo kwa amene ali pa ulendo atha kupaka usana utatu ndi usiku wake (ma ola 72) ngati mtunda wa ulendowo ndi mtunda woti atha kupungula Swalaat mtunda wokwanira 85 km.

**KUYAMBA KWA KUPAKA:** Kupaka kumayamba ukangoduka wudhu pambuyo povala makhuf awiriwo mpaka kudzafika nthawi ngati yomweyo mawa lake kwa munthu amene sali pa ulendo (ma ola 24).

**MLINGO WOMWE UNGAPAKIDWE PA MAKHUF AWIRI:** Malo ochuluka pamwamba pake kuchokera ku zala za miyendo yake mpaka kukatumba wake, ndipo kupakako kukhale ndi zala za manja ake zili zokanukana.

**NDEMANGA:** Amene wapaka ali pa ulendo kenako nkukhala ulendowo kapena anapaka asali pa ulendo kenako nkunyamuka ulendo, kapena anakaika za kuyamba kupaka; adzapaka ngati munthu amene sali pa ulendo.

**TCHIKA (BANDEJI):** Timeneto ndi timitengo tomwe mafupa amalumikizidwa ndi timeneto ndi zofanana ndi mitengoyo, choncho zikuloledwa kupaka pamwamba pake ngati pali zofunikira zingapo: **1)** Ngati akufunika kugwiritsa ntchito bandejiyo. **2)** Isapitirire malo wofunika kumanga bandeji. **3)** Atsogozane pakati pa kupaka pa bandejiyo ndi ziwalo zotsala pochita wudhu. Ngati bandejiyo yapitirira malo wofunika kumanga padzafunika kuchotsa kwa

onjezerekako, koma ngati ataopa vuto pochita zimenezo kudzamkwanira kungopaka pamwambapo.

**PHINDU:** ✸ Popaka pamwamba pa khuf ndibwino kupakira limodzi mosatsogoza kumanja. ✸ Sizili sunnat kupaka pansi pa khuf kapena ku chidendene chake. ✸ Ndi Makrooh kusambitsa makhuf awiri m'malo mopaka ndinso kubwerezabwereza kupaka. ✸ Nduwira ndi mipango n'zofunika kupaka mbali yochuluka ya zinthu ziwirizi.

**ZINTHU ZOONONGA WUDHU: 1)** Chomwe chingatuluke kuchokera pa malo otuluka mkodzo ndi chimbudzi, ngakhale chili cha Twahir ngati mpweya ndi umuna, kapena cha najisi ngati mkodzo ndi madhiyy omwe ali madzi olenda omwe amatuluka ku maliseche chifukwa chachilakolako chogonana. **2)** Kuchoka nzeru chifukwa cha tulo kapena kukomoka, kupatula tulo tochepa togona ali chikhalire kapena chiimire tulo timeneto sitiononga wudhu. **3)** Kutuluka mkodzo kapena chimbudzi kudzera pa malo pena posakhala potulukira pake. **4)** Kutuluka chinthu cha Najisi chosakhala mkodzo ndi chimbudzi kuchokera m’thupi mwake ngati chitatuluka kwambiri monga magazi ambiri. **5)** Kudya nyama ya ngamira. **6)** Kukhudza maliseche ndi dzanja popanda chotchingira. **7)** Kukhudza maliseche achimuna kwa munthu wamkazi, kapena mwamuna, kukhudza maliseche achikazi mwa chilakolako popanda chotchinga. **8)** Kutuluka M’Chisilamu. Ndipo amene watsimikiza kuti ali ndi Twaharat ndipo wakaika zoti alibe Twaharah, kapena anatsikimiza kuti alibe Twaharat ndikukaika zoti ali ndi Twaharat adzatsatira mbali yomwe watsimikizayo.

## GHUSL KUSAMBA THUPI LONSE

**ZOMWE ZIMAPANGITSA KUFUNIKA KUSAMBA: 1)** Kutuluka umuna momva kukoma kwa munthu amene ali maso kapena kutuluka umuna kwa munthu amene ali mtulo momva kukoma kapena mosamva kukoma. **2)** Kulowetsa umaliseche wa mamuma ku maliseche kwa munthu wamkazi ngakhale kuti sanatulutse umuna. **3)** Kusinguka kwa kafiri ngakhale amene anatuluka Chisilamu. **4)** Kutuluka magazi a Haidh. **5)** Kutuluka magazi a Nifaas. **6)** Imfa ya Msilamu.

**ZOFUNIKA PA KUSAMBA:** Zikukwanira kukwanitsa madzi thupi lonse ndi niyyat yakusamba mkamwa ndi m'mphuno.

**Kusamba kumakwanira ndi zinthu zisanu ndi zinai izi: 1)** Achite niyyat ya kusamba. **2)** Anene Bismillah. **3)** Asambitse manja ake awiri asanalowetse zikhathozo m’chiwiya. **4)** Achape maliseche ake ndi zimene malisechewo adzola. **5)** Achite wudhu. **6)** Adzithire madzi pa mutu pake katatu. **7)** Athire madzi pathupi pake. **8)** Anyule thupi lake ndi manja ake awiri. 9) Ayambirire kumanja.

**ZOMWE ZILI HARAAM KWA MUNTHU AMENE ALIBE WUDHU:**

**1.** Kukhudza msahafu. **2.** Kuswali. **3.** Kuchita TWAWAAF Kaabat.

**ZOMWE ZILI HARAAM KWA MUNTHU AMENE ALIBE TWAHARAT CHIFUKWA CHA HADATH YAIKULU**

**1.** Kukhudza Msahafu. **2.** Kuswali. **3.** Kuchita TWAWAAF Kabat. **4.** Kuwerenga Quràn. **5.** Kukhala mu mzikiti asadachite udhu.

Ndipo zili Makrooh: Kugona ndi janaba popanda kuchita udhu ndi kuononga madzi powagwiritsa ntchito.

**TAYAMMUM:**

**ZOFUNIKIRA ZAKE: 1.** Kuvuta kugwiritsa ntchito madzi. **2.** Ichitike ndi dothi la Twahir, lololedwa lokhala ndi fumbi, losaotchedwa.

**NSICHI ZAKE**: Kupaka nkhope yonse, kenako zikhatho ziwiri mpaka mu mphindi zake ziwiri, kulondoloza ndi kuwirikiza.

**ZOMWE ZINGAONONGE TAYAMMUM: 1.** Chilichonse chomwe chingaononge Wudhu. **2.** Kupezeka kwa madzi ngati anachita Tayammum chifukwa cha kusowa madzi. **3.** Kuchoka chomuloleza kuchita Tayammum monga amene anachita Tayammum chifukwa cha kudwala ndipo wachira.

**SUNNAT ZAKE**: **1.** Kulondoloza ndi kuwirikiza pa Tayammum ya chifukwa cha Hadath yaikulu. **2.** Kuchedwetsa kuchita Tayammum mpaka kumapeto kwa nthawi. **3.** Kuwerenga ma Duàa a wudhu pambuyo pake.

**ZOMWE ZILI MAKROOH PA TAYAMMUM:** Kubwereza kumenyetsa zikhatho pa dothi.

**KACHITIDWE KA TAYAMMUM:** Achite niyyat kenako anene Bismillah, ndipo amenye dothi ndi manja ake awiri kamodzi, kenako moyambirira apake nkhope yake popaka ndi mkati mwa zikhatho zake ziwiri ku nkhope kwake ndi ndevu zake, kenako apake ndi zikhatho zake ziwiri pamwamba pa chikhatho chake chakumanja papakidwe ndi mkati mwa chikhatho chake cha kumanzere, ndipo pamwamba pa chikhato cha manzere papakidwe ndi mkati mwa chikhatho chakumanja.

**KUCHOTSA NAJISI:** Manajisi ali mitundu iwiri;

**1) Chomwe chili najisi chenichenicho:** Chimenecho ndi chimene choti n'chosatheka kuchiyeretsa monga nkhumba, choncho ingasambitsidwe maka siikhala ndi twahaarat.

**2) Hukmiyyat:** Iyi ndi imene yachita kufika pamalo amene chiyambi chake ndichoyera monga nsalu, dothi ndipo zili motere:

| ZINTHU | LAMULO LAKE | |
|---|---|---|
| ZINYAMA | MANAJISI | Galu ndi nkhumba, ndi zomwe sizidyedwa m'gulu la mbalame ndi zinyama zomwe zikuposera pa msinkhu wa mphaka kalengedwe kake. Lamulo lake: chenichenicho komanso ziwalo zake zonse ndi zotuluka m'menemo monga mkodzo wake,ndowe zake,malovu ake,umuna wake, mkaka wake, mamina ake ndi masanzi ake. |
| | ZATWAAHIR (ZOYERA) | **1)** Munthu: Lamulo lake:Zonse zotuluka mwa iye zili twaahir (zoyera) monga umuna wake, thukuta lake,malovu ake, mkaka wake, mamina ake, chinyontho chakumalo obisika a mkazi chili twaahir kupatula mkodzo, chimbudzi, madhiyy, wadiyy ndi magazi zimenezi ndi najisi. **2)** Zomwe nyama yake imadibwa. Lamulo lake:Zonse zotuluka m'menemo zili twaahir monga mkodzo wake,ndowe zake, umuna wake, mkaka wake, thukuta lake, malovu ake, masanzi ake komanso madhiyy ake. **3)** Zomwe zili zovuta kuzipewa monga bulu, mphaka ndi zomwe zikuchepera pa msinkhu wa mphaka monga khoswe ndi zina zotero. Lamulo lake: malovu ake ndi thukuta lake basi ndizomwe zili twaahir. |

| | |
|---|---|
| **ZIBUDU** | Zonse ndi najisi kupatula mtembo wa munthu, chibudu cha nsomba ndi dzombe komanso zomwe zilibe magazi womayenderera monga namkalizi, ntchentche, udzudzu ndiye kuti zili twaahir. |
| **ZOPANDA MOYO** | Dothi, miyala ndi zina zotero. Lamulo lake: Zonsezo zili twaahir (zomwe zipatulidwe m'menemo ndi zinthu zimene zatchulidwa kale zija) |

**PHINDU:**

- Magazi, mafinya opanda magazi ndi amagazi omwe zonsezi ndi najisi, ndipo zimakhululukidwa pa Swalaat ndi pa zina zotero zikakhala zochepa zochokera m'nyama za Twahir.
- Magazi a Twaahir opezeka m'mitundu iwiri:

**i.** Nsomba.

**ii.** Magazi otsalira mu nyama ndi m'mitsempha yake kuchokera m'chinyama chozingidwa.

- Mnofu womwe wadulidwa kuchokera m'nyama yomwe imadibwa iyo ili ya moyo, ntchintchi ya magazi ndinso mnofu zonsezo ndi najisi.
- Kuchotsa najisi sikusowekera niyyat, choncho ngati najisiyo itachoka ndi madzi a mvula mwachitsanzo , ndiye kuti najisi imeneyo yayeretsedwa.
- Kukhudza najisi ndi dzanja kapena kuiponda sikuononga wudhu , koma kuti idzafunika kuchotsa komanso kuichotsa yomwe yagwera pa thupi ndi pa nsalu kuchokera mu najisiyo.
- Idzayeretsedwa najisi pakapezeka zofunikira izi:

**1.** Ichapidwe ndi madzi a Twahoor (madzi oyera) wotheka kuyeretsera chinthu china.

**2.** Chifinyidwe chinthu chochapidwacho kunja kwa madzi ngati chili choti chitha kufinyidwa.

**3.** Ichotsedwe najisi poikhula ndi zofanafana ndi kukhulako ngati sikunakwanire kuchapako.

**4.** Ichapidwe kasanu ndi kawiri ndipo kachisanu ndi katatu kachapidwe ndi dothi kapena sopo ngati najisiyo ili ya galu.

**ZIDZIWITSO:**

Najisi ikakhala pa nthaka ngati inali yamadzi monga mkodzo ndiye kuti ikukwanira kuimiza ndi madzi kufikira najisiyo itachoka mtundu wake ndi fungo lake, ndipo ngati najisiyo ili chinthu chooneka ndi maso monga chimbudzi ndiye kuti padzafunika kuchotsa najisi yeniyeniyo ndi chizindikiro chake.

- Najisi ikavuta kuichotsa pokhapokha ndi madzi ndiye kuti idzafunika kuichapa ndi madziwo.
- Akasowa malo amene agwera najisi achapidwe malowo kufikira atatsimikiza kuti aichapa najisiyo.
- Amene wachita wudhu kuti aswali nafI akuloledwa kuti aswali fardh ndi wudhu umenewo.
- Sizili waajib kwa munthu amene wagona kapena waphwisa kuti apange Istinjaa, chifukwa mpweya uli Twahir, koma ayenera kuchita wudhu ngati akufuna kuswali kapena kuchita zina zake zofunika kuchita wudhu.

# MALAMULO AMAYI

## MALAMULO A MAGAZI ACHILENGEDWE A AKAZI LOYAMBA: HAIDHU NDI ISTIHAADHWA

| MAS-ALAT | LAMULO LAKE |
|---|---|
| Kuchepa ndi kuchuluka kwa zaka zomwe angayambire kuchita Hidhwi munthu wa mkazi | Kuchepa kwa zaka zoyambira Hidhwi ndi zaka zisanu ndi zinayi, choncho ngati magazi atatuluka kuchokera ku maliseche ake zisanakwane zaka 9 imeneyo ndi Istihadhwa (matenda wamba). Ndipo kuchuluka kwa zaka zoyambira Hidhwi kulibe malire. |
| Kuchepa kwa masiku amene Hidhwi imapitirira | Usiku ndi usana pa maola 24, choncho ngati itachepera pamenepo ndiye kuti ndi Istihadhwa. |
| Kuchuluka kwa masiku amene Hidhwi imapitirira | Masiku khumi ndi asanu , choncho ngati ataonjezereka magazi ochuluka pa chiwerengero chimenechi ndiye kuti amenewo ndi matenda wamba. |
| Twaharat yokhala pakati pa Hidhwi ziwiri | Masiku khumi ndi atatu , choncho ngati ataoneka magazi chisadakwanire chiwerengero chimenechi ndiye kuti amenewo ndi matenda wamba (Istihaadhwa).(1) |
| Kawirikawiri akazi amachita Hidhwi | Masiku asanu ndi limodzi kapena asanu ndi awiri. |
| Kawirikawiri akazi sachita Hidhwi | Makumi awiri mphambu zitatu kapena makumi awiri mphambu zinayi. |
| Kodi magazi otuluka m'nyengo ya mimba ndi Hidhwi? | Magazi omwe amatuluka kuchokera mwa mkazi amene ali ndi mimba monga magazi ofira modera, kapena ooneka mwa chidothi, kapena ooneka mwa chikasu, magazi oterewo ndi matenda wamba. |
| Wochita Hidhwi adzazindikira liti kuti wamaliza? | **Akazi ali pawiri**: **(1)** akaona zoyera zikutuluka. **(2)** kuuma kwa magazi ofira, achidothi ndi achikasu kumaliseche ngati anali m'gulu la omwe satulutsa zoyera. |
| Zomwe zimatuluka kuchokera ku maliseche a munthu wamkazi mu zinthu zoyenderera mkatikati moti sali pa Hidhwi | Zikakhala zopyapyala , kapena zoyera , zolenda ndiye kuti zimenezo zili Twahir ndipo zikakhala magazi , kapena za mtundu wa chidothi, kapena zachikasu zimenezo ndi najisi ; ndipo zonsezo zimaononga wudhu ndipo zikapitirira kutuluka kwake ndiye kuti amenewo ndi matenda wamba. |
| Za mtundu wachidothi kapena wachikasu zotuluka kuchokera ku maliseche | Ngati zalumikizana ndi Hidhwi , zatuluka Hidhwi isanatuluke kapena pambuyo pake ndiye kuti nazonso ndi Hidhwi , ndipo zomwe zalekana ndi Hidhwi ndiye kuti ndi matenda wamba |
| Amene ali ndi masiku ochitira Hidhwi mwezi ulionse ndipo Hidhwiyo yasiya asanakwane masikuwo | Mkazi ameneyo zidzagamulidwa pa iye kuti Hidhwiyo yaleka ngati magazi atasiya kutuluka ndipo waona kuti wayera ngakhale kuti sanathe masiku ake a Hidhwi omwe anazolowera kuwaona magazi m'masiku amenewo. |

---

[1] **ISTIHADHWA**: Amenewo ndi magazi a matenda wamba amachucha kuchokera mu mtsempha wa kunsi kwa chiberekero. Ndipo kusiyana kwa pakati pa magazi a hidhwi ndi Istihadhwa ndi uku:

**1.** Magazi a hidhwi amakhala ofira modera, ndipo magazi a Istihadhwa ndi ofira mowala ngati magazi a kamfuno.

**2.** Magazi a hidhwi amakhala ochindikala, ndipo nthawi zina amatsagana ndi kupweteka m'mimba. Tsopano magazi a Istihadhwa amakhala opyapyala amachucha ngati akuchokera pa bala.

**3.** Magazi a hidhwi nthawi zambiri fungo lake limakhala lonyasa, lonunkha .Tsopano magazi a Istihadhwa fungo lake limakhala ngati la magazi wamba .Tsopano kumbali ya malamulo: amene ali pa hidhwi zili Haraam kwa iye zomwe zili Haraam kwa amene ali ndi Hadath yaikulu monga kuswali, kukhala mu mzikiti, kuwerenga Quràn, kumanga swaum ndi zina zotero.

| | |
|---|---|
| Hidhwi yafulumira nthawi yake yachizolowezi isanakwane kapena yachedwa mopitirira nthawi yake | Akaonera m'menemo maonekedwe a Hidhwi; ndiye kuti ndi Hidhwi mu nthawi ina iliyonse , koma pafunikira kuti pakhale masiku ochuluka kupitirira masiku khumi ndi atatu pakati pa Hidhwi ziwiri omwe ali masiku ochepa amene sakhala ali ndi Hidhwi, ndipo ngati sakukwanira masiku amenewo ndiye kuti ndi matenda wamba. |
| Hidhwi ikaonjezereka kapena kupunguka m'masiku a chiwerengero chake cha chizolowezi | Imeneyo ndi Hidhwi, koma pafunikira kuti chiwerengerocho chisaonjezere pa masiku ochuluka a Hidhwi omwe ndi masiku khumi ndi asanu. |
| Mkazi akatulutsa magazi nthawi yaitali monga mwezi wathunthu kapena kupitirira apo | **Mkazi ameneyo ali mu gulu limodzi mwa magulu awa:**<br>**1)** Amene akudziwa nthawi yake ya Hidhwi pa mwezi ndi chiwerengero cha masiku ake ndipo amasiyanitsa pakati pa magazi a Hidhwi ndi ena; ndiye kuti adzagwiritsa ntchito chiwerengero ndi nthawi ya chizolowezi osati ndi maonekedwe a magazi chimodzimodzi magazi ake ndi wodziwika kapena ayi.<br>**2)** Amene akudziwa nthawi yake ya Hidhwi pa mwezi koma sadziwa chiwerengero cha masiku ake ndiye kuti ameneyo adzakhala masiku asanu ndi limodzi kapena asanu ndi awiri omwe kawirikawiri Hidhwi imachitika<br>**3)** Amene amadziwa chiwerengero cha masiku a Hidhwi yake koma sadziwa nthawi ya kubwera kwake pa mwezi ndiye kuti ameneyo adzakhala pa chiwerengero chomwe akudziwa kumayambiriro kwa mwezi ulionse wa chithunzi |

## LACHIWIRI: "NIFAAS"MAGAZI OTULUKA PAMBUYO PA KUTHA KUBEREKA

| MAS-ALAT | LAMULO LAKE |
|---|---|
| Mayi akabereka ndipo sanatulutse magazi | Satsatira malamulo a amayi amene ali ndi nifaas ndipo sizili waajib kwa iye kusamba pathupi, ndipo swaum yake siingaonongeke |
| Akaona zizindikiro za kubereka | Zomwe amaziona monga magazi ndi madzi zikupweteka kwa kanthawi kochepa asanabereke zimenezo sizingatenge malamulo a Nifaas koma a matenda wamba |
| Magazi omwe amatuluka mwa mkazi pa nthawi yomwe akubereka | Magazi amenewa ndiye Nifaas, ngakhale asanatuluke mwana kapena watuluka mbali ina, ndipo sizili waajib kwa mkazi ameneyu kubweza Swalaat yomwe yam’dutsa pa nthawi imeneyo. |
| Kodi kuwerengera masiku a Nifaas kumayamba nthawi yanji? | Pambuyo pa kumalizika kubadwa khanda mpaka pansi kuchokera m'mimba mwa mayi wake |
| Kodi kuchepa kwa nthawi ya Nifaas kuli bwanji? | Kuchepa kwake kulibe malire , choncho ngati atabereka kenako pambuyo pake nthawi yomweyo n'kusiya kutuluka magazi zidzakhala waajib kuti asambe ndi kuswali kupatula akakumana ndi nthawi ya haidhwi. |
| Kodi kuchuluka kwa nthawi ya masiku a nifaas kuli bwanji? | Ndi masiku makumi anayi, choncho akaonjezereka asawagwiritse ntchito ndipo ndi waajib kuti asambe ndi kuswali pokhapokha ngati yagundana ndi nthawi ya Hidhwi yake asanatenge mimba, ndiye kuti idzawelengedwa kuti ndi Hidhwi |
| Amene wabereka ana awiri kapena kuposera apo | Kuwerengera kwa masiku a Nifaas kudzayamba pambuyo poti mayi wabereka mwana woyamba |
| Magazi otuluka | Ngati msinkhu wa mtayowo uli masiku makumi asanu ndi atatu (80) kapena kuchepekera apo ndiye kuti magazi omwe angatuluke pambuyo pake adzakhala |

| | |
|---|---|
| pambuyo pa mtayo | matenda wamba koma akatuluka pambuyo pa masiku makumi asanu ndi anayi (90); ndiye kuti magazi otuluka pambuyo pake adzakhala Nifaas .Ndipo mtayowo ukakhala pakati pa masiku makumi asanu ndi atatu (80), ndi masiku makumi asanu ndi anayi (90) ndiye chigamulo chidzagwirizana ndi kalengedwe, choncho chomwe chili ndi kalengedwe ka munthu, ndiye kuti magazi otuluka pambuyo pake ndi nifaas ndipo ngati sadaleke adzakhala matenda wamba. |
| Magazi akasiya kutuluka mkatikati mwa masiku makumi anayi, kenako nkubweranso masiku makumi anayi asanakwanire | Kusiya kutuluka magazi komwe mayi angakuone mkatikati mwa masiku makumi anayi a Nifaas kumeneko ndi kuyera ndithu, mayiyo asambe ndikuswali ndipo akabweleranso kutulutsa magazi mkatikati mwa masiku makumi anayi pamenepo adzatsatira malamulo a Nifaas, ndipo zidzakhala choncho kufikira kutha kwa masiku makumi anayi. |

**IMVANI IZI**

- Zili waajib kwa mayi wa Istihadhwa kuti aswali; koma kuti iye azichita wudhu pa Swalaat iliyonse.
- Mayi akasiya kuchita hidhwi kapena nifaas dzuwa lisanalowe akukakamizidwa kuti aswali Zuhr ndi Asr ya tsiku limenelo, ndipo akasiya m'bandakucha usanatuluke ndiye kuti iye aswali Maghrib ndi Isha ya usiku umenewo.
- Mayi ikamkwanira nthawi ya Swalaat kenako n'kuyamba hidhwi kapena nifaas asanaswali Swalaatyo ndithu akukakamizidwa kuchita Qadhwa.
- Zili waajib kwa mayi kumasula tsitsi lake pamene akusamba chifukwa cha hidhwi kapena Nifaas, ndipo sizili waajib kumasula tsitsilo ngati akusamba chifukwa cha Janaabat.
- Ndi makrooh kugonana ndi mayi wa Istihadhwa ndipo zikuloledwa kwa mwamuna kugonana naye ngati patafunika kutero.
- Zili waajib kwa mayi wa istihaadhwa kuchita udhu pa Swalaat ili yonse pambuyo pakusamba kwake chifukwa chakuchita hidhwi ndipo zitero kufikira magazi atasiya.
- Zikuloledwa kwa mayi kugwiritsira ntchito mankhwala oletsa hidhwi mwa kanthawi kochepa kuti achite mapemphero a Hajj ndi umrat, kapena kuti akwaniritse Swaum ya Ramadhan, koma zimenezo zifunikira kuti akhale ndi chitetezo choti mankhwalawo sangapereke vuto.

# MAYI M'CHISILAMU

Mayi ali wofanana ndi mwamuna polandira malipiro komanso ubwino kwa Allah molingana ndi chikhulupiriro ndi ntchito. Mtumiki (SAW) adati: "*Ndithudi mayi ndi m'bale wa mwamuna*." **Abou Daood**. Ali ndi ufulu woitanitsa ufulu wake kapena kuchotsa kupondereza kumene kwamugwera. Zili dero chifukwa kuyankhula kwa chipembedzo kumapita kwa mayi komanso bambo onse limodzi kupatula malembo amene abwera posiyanitsa pakati pawo, awa ndi malamulo ochepa tikafanizira ndi malamulo otsalawo. Izi ndi chifukwa chakuti malamulo a Chisilamu amasamalira kwambiri zosankhika za mwamuna ndi mkazi poganizira kalengedwe ndi kuthekera. Allah (SW) wati: "*Kodi asazindikire amene adalenga kumachita Iye ndi Wodekha, Wozindikira*?" Mayi ali ndi ntchito zimene zimaamukhudza ndiponso mwamuna ali nazo zina zokhudza iye choncho kulowerana kulikonse pa ntchito zokhudza wina, zimadzetsa mavuto pakukhazikika kwa moyo. Komanso mayi amapatsidwa malipiro ofanana ndi mwamuna mayiyo ali chikhalire pa nyumba pake. Hadith wailandira Asmaa' Bint Yaziid (RA) ndithudi iye adam'pitira Mneneri (SAW) ali pakati pa maswahaaba ake iye nane kuti: "*Ndichitira nsembe makolo anga awiri pa iwe! Ine ndine nthumwi ya amayi kwa iwe - ndikutinso ndiphunzire – kwa iwe tapereka moyo wathu. Ndithudi palibe mayi aliyense kulikonse ali kaya kuvuma kapena kuzambwe amene wamva kapena ayi za kutuluka kwangaku pokhapokha ali ndi maganizo ngati angawa. Ndithu Allah adakutumiza ndichoonadi kwa amuna komanso amayi ndipo tidakukhulupirira iweyo komanso Allah wako amene adakutumiza. Ndithudi ife akazife tili omangika -okhazikika- pa nyumba zanu, pothera zilakolako zanu,timatenga mimba za ana anu ndipo inu abambo mwatiposa ife poswali Jum'a, Swalaat ya pa gulu (jamaat), kukaona odwala, kukakhala nawo pa mwambo wa maliro, kuchita mapemphero a Hajj pambuyo pa inzake, kuposera apa kukachita jihaad mu njira ya Allah. Ndithudi munthu wamwamuna mwa inu akatuluka kupita kukachita Hajj kapena Umrat kapenanso ku usirikali kukalondera malire, ife timakusungirani chuma chanu, kukupeterani zovala zanu, kukulererani ana anu ndiye ndi malipiro anji amene tikuwapeza limodzi ndi inuyo eh iwe Mtumiki* (SAW)? (Wokamba Hadithyi) adati:ndipo Mneneri (SAW) adatembenukira kwa maswahaaba ake ndi nkhope yake yonse kenako adati: "*Kodi mudayamba mwamvako mawu amayi abwino ndikufunsa kwake kwa zinthu zokhudza chipembedzo chake kuposa uyu?"* Iwo adati: 'Eh iwe Mtumiki (SAW) wa Allah! Sitimaganiza kuti mmayi angawongoke ku zonga izi.' Kenako Mneneri (SAW) anatembenukira kwa mzimayiyo nanena kwa iye kuti: "*Zipita iwe mzimayi, ndipo ukawadziwitse amayi amene wasiya pambuyo pako kuti ndithu kukhala mkazi wabwino kwa mmodzi wa inu kwa mwamuna wake, ndi kufuna kwake chiyanjo chake,ndi kutsatiratsatira kwake zoyanjana ndi mwamunayo, zikufanana ndi zonse zija (zimene amuna akuchita)*". Iye (wonena Hadithyi) adati: '*Ndiye mzimayi uja adatembenuka akunena kuti: 'Laailaaha Illa Allah , Allah akbar! Kusangalalira zimenezi*" **Al Baihaqiyy**. Ndipo adafika amayi kwa Mtumiki (SAW) nati: "*Atsogola abambo ndi ubwino pochita jihaad mu njira ya Allah, kodi tiribe ntchito zina zimene tingawafikire nazo ntchito za amuna ochita jihaad mu njira ya Allah*?" Ndiye Mtumiki (SAW) wa Allah adati: "*Ntchito za manja za mmodzi wa inu pa nyumba pake amafika nazo ntchito ya anthu*

*ochita jihaad mu njira ya Allah*." **Al Baihaqiyy**. Koma kuti Chisilamu chachita kuchitira zabwino m'bale wachikazi kuti ali nawo malipiro aakulu munthu woteroyo. Adayankhula (SAW) kuti: "*Munthu amene wasamalira ana awiri achikazi kapena alongo awiri kapena achibale achikazi awiri, uku akumadziwerengera chisamaliro pa iwo kufikira Allah atawakwaniritsa kapena atawalemeretsa ndi zabwino Zake, akakhala awiri amenewo chomutsekereza iye ku moto*." **Ahmad, Al Tabariyy**.

## MALAMULO ENA A AZIMAYI

✷ **Ndizoletsedwa** mwamuna kukhala mseri ndi mayi amene pakati pake ndi iye palibe ubale woletsa kukwatirana (monga: bambo, agogo aamuna angakhale mtundu wawo utakwera, mwana wamwamuna, chidzukulu chamwamuna,mwana wako angakhale mtundu utatsika, mchimwene ndi ana awo achimuna, bambo, mwana ndi mchimwene chifukwa choyamwira bere limodzi, mwamuna wa mwana wako wamkazi ndi mwamuna wa amayi ako. Mtumiki (SAW) adati: "*Asakhale mseri limodzi bambo ndi mayi pokhapokha patakhala munthu woti sangakwatirane naye*." **(Bukhar, Muslim).**

▪ **Ndizovomerezeka mayi** kuswalira mu mzikiti, koma ngati ataopa mayeserero ndiyeno kukhala makrouh. Adanena Aishat (RA) kuti : "*Adakakhala Mtumiki (SAW) adazipeza zimene amayi azipeka pano, bwenzi ataletsa kupita ku mzikiti monga m'mene adawaletsera ana a Israel*." **(Bukhar, Muslim).** M'mene ilili Swalaat ya mwamuna kuti imaonjezereka malipiro ake, chimodzomodzinso Swalaat ya mayi (imaonjezerekanso) akaipempherera m'nyumba mwake. Adabwera mayi kwa Mneneri (SAW) nanena kuti: "*Ine ndikukonda kumaswali nawe*." Iye (SAW) adati: "*Ndithu ine ndadziwa kuti ukukonda kuswali limodzi nane koma Swalaat yako m'nyumba mwako ndiyabwino kuposa Swalaat yako m'chipinda mwako mogona. Ndipo Swalaat yako m'chipinda mwako mogona ndi yabwino kuposa Swalaat yako m'nyumba mwako. Ndipo Swalaat yako m'nyumba mwako ndi yabwino kuposa Swalaat yako mu mzikiti wa anthu akwanu. Ndipo Swalaat yako mu mzikiti wa anthu akwanu, ndi yabwino kwambiri kuposa Swalaat yako mu mzikiti wanga*." **Ahmad**. Ndiponso Mtumiki (SAW) adati: Malo wopempherera abwino kwa mayi ndi nyumba zawo." **Ahmad**. Siziri waajib kwa mayi kukachita Hajj kapena Umrat pokhapokha atapeza munthu woti sangakwatirane naye kuti amuperekeze pa ulendowo. Ndipo ndizosavomerezeka ulendo wa mayi popanda munthu amene sangakwatirane naye chifukwa chakuyankhula kwake (SAW) koti: "*Asayende mayi ulendo pamwamba pa masiku atatu, pokhapokha atakhala limodzi ndi munthu amene sangakwatirane naye*." **(Bukhar, Muslim).**

✷ **Zili** haraam kwa mayi kukazonda manda (ziyaarat) ndikuperekeza janaazat chifukwa cha kuyankhula kwa Mtumiki (SAW) koti: "*Allah awatemberera amayi ochulukitsa kukaona manda*." Ndipo Ummu Atwiyyat (RA) adati: "*Tidaletsedwa kutsatira janaazat koma sizidakakamizidwe pa ife*." **(Muslim).**

✷ **Ndizovomerezeka** kwa mayi kusandutsa tsitsi lake la m'mutu ndi mtundu wina uli wonse koma zimakhala makrouh kulisandutsa ndi zakuda ndi chofunikira chakuti kuteroko kulibe chinyengo kwa munthu wodzafunsira mbeta.

✷ **Ndiwaajib** kupatsidwa mayi gawo lake limene Allah adamuikira mu chuma cha ulowammalo (chamasiye), ndipo ndi haraam kumumana gawolo. Kwafika nkhani

kuchokera kwa Mtumiki (SAW) kuti adati: "*Amene wadula chuma cha ulowammalo (chamasiye) Allah adzadula ulowammalo wa iyeyo ku Jannat tsiku la Kiyaamat*." **(Ibn Maajah).**

✷ **Zili** waajib kwa mwamuna kupatsa mkazi wake zinthu zimene nkosatheka kukhala alibe monga chakudya, chakumwa, chovala ndi malo wokhala mwaubwino. **Allah** wanena kuti: "*Adzipereka (chisamaliro kwa mkazi) yense wokhala ndi danga kuchokera mu danga lake, ndipo amene wachepekedwera kwa iye rizq lake azipereka mu zomwe Allah wamupatsa*." Ngati mayiyo ndi wopanda mwamuna ndiye zili waajib kwa bambo ake kapena mchimwene wake, kapena mwana wake wa mwamuna kumupatsa chisamaliro. Ngati alibe wachibale aliyense ndiye zikhala sunnat kwa anthu ena onse kumupatsa chisamaliro chake chifukwa cha Hadith iyi: "*Amene akukangalika kusamalira mayi wamasiye ndi munthu wosowa ali ngati amene akuchita jihaad mu njira ya Allah kapenanso ali ngati munthu amene amaima kuswali usiku onse komanso kumanga masana*." **(Bukhar, Muslim).**

✷ **Mzimayi** ndiwoyenerera kulera mwana wake wamng'ono ngati asanakwatiwe. Ndizofunikira kwa bambo a mwanayo kum'patsa mayi wamwanayo chisamaliro chonse mmene akhalire mwanayo m'manja mwake.

✷ **Sizili** sunnat mkazi kuyamba kupereka salaam makamaka akakhala wachitsikana kapena akuopedwera mayeserero.

✷ **Zili** sunnat kumeta tsitsi la kumalo ake wobisika,kuchotsa tsitsi la kunkhwapa ndi kuwenga zikhadabwe tsiku la Ijuma lili lonse. Zili makrouh kuzisiya zimenezi m'masiku oposera makumi anayi (40).

✷ **Zili** haraam kudula tsitsi la kunkhope -mwa ilo- nsidzi chifukwa Mtumiki (SAW) adati: "*Allah adatemberera mayi wochotsa nsidzi ndi amene akuchotsetsa*." **(Aboo Daood).**

✷ **KULIRA MALIRO:** Zili haraam kwa munthu wamkazi kulira maliro a wina wake kopitirira masiku atatu, kupatula maliro a mwamuna wake, pakuti maliro a iye, mkaziyo ayenera kulira miyezi inayi ndi masiku khumi, ndipo polira malirowo ayenera kusiya kudzikongoletsa ndi zonunkhira, monga Zafaran, kuvala zodzikongoletsera ngakhale mphete kumene, zovala za mitundu yokongola monga za mtundu wofiira ndi wa chikasu, komanso kudzikongoletsa ndi hanna, kapena kudaya, kapena kupaka m'maso wanja wakuda, kapena kudzola mafuta onunkhira. Ndipo akuloledwa kuwenga makadabo, kuzula tsitsi komanso kusamba. Ndipo palibe mtundu weniweni wa chovala wofunika monga wakuda. Ndipo zili waajib kukhala pa chiyembekezo pa nyumba pomwe mwamuna wake wamwalirira mkaziyo ali m'menemo, ndipo zili haraam kusintha nyumbayo pokhapokha ngati zitafunika kutero, ndipo asatuluke m'nyumba yake masana pokhapokha ngati pali chifukwa.

✷ Ndi haraam kwa mayi kumeta tsitsi la m'mutu wake popanda chifukwa cheneicheni, ndizovomerezeka kuliyepula koma kudzera muchofunikira choti asadzifananize ndi amuna chifukwa cha Hadith iyi; "*Mtumiki wa Allah adatemberera amayi odzifananiza ndi amuna m'gulu la amayi*." **Tirmidhi**. Kapena kudzifananiza ndi makafir achikazi chifukwa cha Hadith iyi: "*Yemwe angadzifananize ndi anthu ena ndiye kuti iyeyo ndi mmodzi wa iwo*. **(Abou Daaood).**

✸ Zili waajib kwa mayi kubisa thupi lonse akamatuluka m'nyumba mwake ndi mkanjo umene ukwaniritse malamulo awa: **1)** Kukwanira thupi lonse. **2)** mwa uwo wokha usakhale chodzikongoletsera. **3)** ukhale wokhuthala wosati wamberewere. **4)** ukhale wotaya wosati wothina. **5)** usakhale wothiridwa mafuta wonunkhiritsa. **6)** usafanane ndi zovala za mwamuna. **7)** usafanane ndi zovala zamakafiri achikazi. **8)** usakhale chovala chotchukira nacho. Ndipo ndi haraam kuvala nsalu ili yonse imene ili ndi chithunzi cha munthu kapena nyama, kupachika, kutchingira pakhoma kapenanso kuigulitsa.

**Maliseche a mayi ndi munthu wina ali mzigawo zitatu: 1)** Mwamuna wake: Ali nako kuyang'ana pa iye paliponse angafune. **2)** Amayi anzake komanso anthu omwe sangamukwatire: Awone mwa iye zomwe zimaonekera nthawi zambiri monga nkhope, tsitsi, khosi, chakhatho, dzanja, phazi ndi zina zotero. **3)** Amuna otsalawo; Asaone mwa iye kena kalikonse kupatula pakakhala chifukwa chenicheni monga: kufunsira mbeta, kuchiza matenda ndi zina zotero. Zili dero chifukwa mayeserero amkazi ali pa nkhope pake. Adanena Faatimat Bint Al Munzir (RA) kuti: "*Tinkavindikira nkhope zathu kwa amuna.*" **Al- Haakim.** Ndipo Aisha (RA) adati: "*Anthu okwera zinyama adali nkumatidutsa ife tili ndi Mtumiki (SAW) titachita ihraam ya Hajj. Iwo akatifupikira , yense wa ife amadzifundira ndi mkanjo wake kuchokera ku mutu kwake mpaka ku nkhope kwake ndipo akatidutsa timachotsa.*" **(Aboo Daaood).**

✸ **ZIYEMBEKEZO**: Ziyembekezo zili m'mitundu ingapo iyi:-

**1)** Chiyembekezo cha amene ali ndi mimba: Chiyembekezo cha mkazi amene mwamuna wasiidwa ukwati ali ndi mimba ndiye kufikira atabereka mimba yakeyo. **2)** Amene mwamuna wake wafa: Chiyembekezo chake ndi miyezi inayi ndi masiku khumi. **3)** Amene wapatsidwa cha mbeta iye akadasamba: Chiyembekezo chake achite hidhwi katatu. Ndipo chiyembekezo chidzatha ndi kusiya kwa hidhwi yachitatuyo. **4)** Amene sasamba (sachita hidhwi chifukwa cha ukalamba kapena sadakule msinkhu): Chiyembekezo chake ndi miyezi itatu. Tsono mkazi wosiidwa kumene kuli kotheka kubwererana naye, ndikokakamizidwa kuti akhalaebe kwa mwamuna wake nthawi yonse ya chiyembekezo ndipo kuli kololedwa kuti mwamuna awone zomwe akuzifuna pa iye, komanso kukhala naye mwa mseri mpaka chiyembekezo chake chitamalizika mwina Allah angayanjanitse pakati pawo. Ndipo kubwererana ukwati nkosasowekera kupezeka chifuniro cha mkazi ngati kusiyana kwake koti nkubwererananso komanso kubwerera ukwati kungachitike ndi mau a mwamuna onena kuti ndakubwerera ukwati; kapena kugonana ndi mkaziyo.

✸ Mayi asadzikwatitse yekha ukwati. Mtumiki (SAW) adati: "*Mayi aliyense wadzikwatitsa yekha popanda chilolezo cha waliyy (muimiriri) wake ndiye kuti ukwati wakewo ndiwoonongeka.*" **Abou Daaood.**

✸ Ndi haraam kwa mayi kulumikiza tsitsi lake ndi tsitsi lina. Komanso ndi haraam kutema mphini zodzikongoletsera pena pali ponse pa thupi lake. Zinthu ziwirizi zili m'gulu la machimo aakuluakulu kwambiri chifukwa chakuyankhula kwa Mtumiki (SAW) koti: "*Allah adamutemberera mayi aliyense wolumikiza tsitsi ndi amene akulumikizitsayo komanso mayi wodula mphini komanso wodzidulitsayo.*" **(Bukhar, Muslim).**

✸ Ndi haraam kwa mayi kupempha kwa mwamuna wake kusiidwa ukwati popanda chifukwa chenicheni chifukwa chakuyankhula kwa Mtumiki (SAW) koti: "*Mayi aliyense angapemphe mwamuna wake kuti amusiye ukwati popanda vuto lili lonse, ndi haraam kwa iyeyo fungo la ku Jannat*." **(Aboo Daaood).**

✸ Ndi waajib kwa mayi kumvera mwamuna wake mwa ubwino makamaka akamuitanira ku mphasa. Adanena (SAW) kuti: "*Mwamuna akaitanira mkazi wake ku mphasa nakana kubwera, mwamunayo nagona ndi mkwiyo, angero amamutemberera mayiyo mpaka atacheredwa*." **(Bukhar, Muslim).**

✸ Ndi haraam mayi kudzithira mafuta wonunkhira akadziwa kuti m'njira, akafikira abambo oti atha kukwatirana nawo chifukwa cha hadith iyi: "*Ndithu mayi akadzithira mafuta wonunkhira, nawadutsa anthu cholinga choti amve fungo lakelo, iye ndiwoteretere – akutanthauza kuti wachiwerewere*." **(Aboo Daaood).**

# SWALAAT

**AZAAN NDI IQAMAH:** Ziwirizi zili Fardh Kifaayat kwa anthu amuna ngati sali pa ulendo, ndipo zili Sunnat kwa munthu woswali yekha komanso kwa wa pa ulendo, ndipo zili makrooh kwa akazi. Ndipo sizingatheke kuchita nthawi ya Swalaat isanakwane; kupatula pa Swalaat ya Fajr nkutheka kuchita Azaan yoyamba ya Fajr pambuyo pa theka la usiku.

**ZOFUNIKIRA ZA SWALAAT: 1)** Chisilamu. **2)** Kukhala ndi nzeru asakhale wamisala. **3)** Akhale wotha kusiyanitsa chabwino ndi choipa. **4)** Twaharat ngati kuli kotheka. **5)** Kukwana nthawi: Ndipo nthawi ya Zuhr imayamba ndi kupendekeka kwa dzuwa mpaka kukhale kutalika kwa mthunzi wa chinthu chilichonse chimodzimodzi ndi chinthucho.
Kenako imayamba nthawi ya Asr, ndipo nthawi yodzisankhira m'menemo ndi mpaka kukhale kutalika kwa mthunzi wa chinthu chili chonse molingana kawiri ndi chinthucho, kenako imakhala nthawi ya pozingwa ndiye mpaka kulowa kwa dzuwa. Kenako imatsatira nthawi ya Maghrib mpaka italowa mitambo yofira. Kenako imayamba nthawi ya Isha, ndipo nthawi yodzisankhira m'menemo ndi mpaka theka la usiku, kenako nthawi ya pozingwa ndiye mpaka kutuluka kwa m'bandakucha woona, ndipo kenako imayamba nthawi ya Fajr, yomwe ndi mpaka kutuluka kwa dzuwa.
**6)** Kubisa umaliseche (ngati pali kuthekera ndi chinthu chosaonetsa mtundu wa khungu; choncho umaliseche wa munthu wamwamuna amene wakwanitsa zaka khumi uli pakati pa mchombo ndi bondo. Ndipo kwa wamkazi amene ali mfulu wotha msinkhu akakhala pa Swalaat thupi lake lonse ndi maliseche kupatula nkhope yake). **7)** Kupewa najisi pa thupi pake, pa nsalu yake ndi pa malo poswalira ngati kuli kotheka. **8)** Kulunjika ku Qiblat ngati kuli kotheka. **9)** Kuchita niyyat.

**NSICHI ZA SWALAAT: Ndipo izo zilipo khumi ndi zinayi:**
**1)** Kuimirira ngati pali kuthekera pa Swalaat ya Fardh **2)** Takbirat yoyamba. **3)** Kuwerenga Faatihah. **4)** Kuwerama pa Rakaat iliyonse. **5)** Kuweramuka kuchokera pa Ruku. **6)** Kuongoka ataimirira pambuyo pa Ruku. **7)** Kuchita Sajdat ndi ziwalo zisanu ndi ziwiri. **8)** Kukhala pakati pa Sajdat ziwiri. **9)** Tashah - hud yomalizira. **10)** Kukhala chifukwa cha Tashah – hud. **11)** Kunena Allaahumma swalli alaa Muhammad.....pa tashahhud yomaliza. **12)** Salaam yoyamba.**13)** Kudekha mu nsichi za zichitochito. **14)** Kuchita molondoloza nsichi zimenezi.

**Ndipo Swalaat singatheke pokhapokha ndi nsichi zimenezi, ndipo Rakaat imaonongeka chifukwa cha kusiya imodzi mwa zimenezi mwadala kapena moiwala.**

**ZOFUNIKA ZA SWALAAT: Zilipo zisanu ndi zitatu:**
**1)** Ma Takbirat onse kupatula Takbirat yoyamba. **2)** Kunena mau oti SamiAllahu liman hamidah amene atanthauza kuti: 'Allah wamumva amene wa mtamanda Iye' kwa Imaam komanso woswali payekha. **3)** Poweramuka kuchokera pa Ruku kunena mau oti Rabbanaa walakal - hamdu: 'Eya, Mbuye wathu, ndipo Inu muli ndi kutamandindwa konse kwabwino'. **4)** Kunena kamodzi pa Ruku mau onena kuti: *Sub - hana Rabbial-Adhweem* 'ulemelero ndi wa Mbuye wanga Wolemekezeka'. **5)** Kunena kamodzi pa Sajdat mau onena kuti: "*Sub -hana Rabbial - A'laa*" ulemerero ndi wa Mbuye wanga Wapamwambamwamba". **6)**

Kunena Du'aa yoti: "*Rabbigh - Firli* omwe atanthauza kuti: "Mbuye wanga ndikhululukireni", pakati pa Sajdat ziwiri. **7)** Tashah - hud yoyambirira. **8)** Kukhala chifukwa cha Tashah - hud imeneyo.

**Ndipo zofunika zimenezi ngati atazisiya mwadala ndiye kuti Swalaat yake yaonongeka, ndipo ngati azisiya moiwala adzachita Sajdat chifukwa cha kuiwalako.**

**SUNNAT ZA SWALAAT:** Pali zoyankhula ndi zochita, ndipo Swalaat singaonongeke chifukwa chosiya chilichonse mu zimenezo ngakhale atasiya mwadala. Choncho Sunnat za pakuyankhula ndi izi: Kuwerenga Du'aa yotsegulira Swalaat, Ta - aw - wudh, Bismillah ndi kunena mau oti Aameen, ndinso kukweza mau ponena Aameen, mu Swalaat yokweza mau powerenga, kuwerenga pomwe papepuka kuchokera mu Quran pambuyo powerenga Faatihat. Kukweza mau powerenga kwa amene ali Imaam, koma otsatira akuletsedwa kutero, pomwe woswali payekha ali ndi kusankha, pambuyo pa Tahmeed kunena mau oti Hamdan katheeran Twayyiban mubarakaatn Feeh, mil - us - samawaat, wamil - ul - Ardh mpaka kumapeto. (Kutamanda kochuluka, kwabwino, kokhala ndi madalitso, kodzadza kumwamba ndi pansi). Zomwe zaonjezereka pa kamodzi m'ma Tasbih apa Ruku ndi pa Sajdat, ndikunena Du'aa yoti: ***Rabbigh - Firli***" yotanthauza 'Mbuye wanga ndikhululukireni', ndikuchita Du'aa asanapereke Salaam.

**NDIPO MA SUNNAT AZICHITOCHITO NDI AWA:** Kutukula manja awiri pochita Takbirat yoyamba, popita pa Ruku, poweramuka kuchokera pa Ruku, ndi ponyamuka kuchokera pa kukhala kwa Tashah - hud yoyamba. Kuika dzanja la manja pamwamba pa dzanja la manzere m'munsi mwa chidali ali chiimire, kuyang'ana kwake pa malo a Sadjat. Kusagundanitsa kwake mapazi ake awiri ataimirira. Pochita Sajdat yake kuyambira kuika maondo ake, kenako manja ake, kenako mphumi yake ndi mphuno yake, kulekanitsa manja ake ndi nthiti zake, mimba yake ndi ntchafu zake, komanso ntchafu zake ndi akatumba ake, kulekanitsa kwake pakati pa maondo ake, kuongola mapazi ake molekanitsa, ndikuika pansi mkati mwa zala zake, kuika manja ake moyang'anizana ndi mapewa ake, zala zili zotambasula zophatana, kuima kwake ndi nsonga za mapazi ake, ndi kuyedzamira kwake pa maondo ake ndi manja ake, kukhalira mwendo pa kukhala kwa pakati pa ma Sajdat awiri ndi pa Tashah - hud yoyamba, kukhalira thako pa kukhala kwachiwiri, kuika manja pamwamba pa ntchafu zala zili zotambasulidwa, zophatana, pakati pa Sajdat ziwiri, chimodzimodzinso pa Tashah - hud: kungoti iye kudzanja la manja adzafumbata kachala kakang'ono ndi kotsatizana nako, ndipo adzazunguliza chala chake chachikulu ndi cha pakati, ndikulozera ndi cha mkombaphala pomutchula Allah ndikuchita kwake Du'aa mosonyeza umodzi wa Allah, kucheukira kwake kumanja ndi kumanzere popereka Salaam, ndi kuyambira kumanja pocheuka.

**KUCHITA SAJDAT CHIFUKWA CHA KUIWALA:** Zili Sunnat kuchita SajdaT Sahw, ngati atabweretsa mau oikidwa mu Swalaat posakhala pa malo pake moiwala monga kuwerenga Qur'an pa Sajdat. Ndipo zikuloledwa kuchita Sajdat Sahw ngati atasiya chinthu cha Sunnat. Sajdat Sahw idzakhala waajib akaonjezera Ruku, kapena Sajdat, kapena kuimirira, kapena kukhala, kapena wapereka Salaam Swalaat isanakwanire, kapena walakwitsa kuwerenga kulakwitsa komwe

kungasinthe tanthauzo, kapena wasiya chinthu cha waajib, kapenanso wakaika za kuonjezera pa nthawi yochita chinthucho. Ndipo Swalaat idzaonongeka chifukwa chosiya mwadala Sajdat Sahw yomwe ili waajib, ngati atafuna atha kuchita Sajdat ziwiri za Sahw asanapereke Salaam, kapena atapereka, ngati ataiwala kupanga Sajdat nkudutsa nyengo yaitali, palibe kupanga Sajdat Sahw.

**KASWALIDWE KA SWALAAT:** Akaima kuti aswali alunjike ku Qiblat ndipo anene kuti **ALLAHUAKBAR**. Imaam akweze mau ponena mau amenewa, komanso ponena ma Takbirat ena onse kuti amve amene ali pambuyo pake ndipo amene sali Imaam asakweze mau ponena ma Takbiratwo. Ndipo atukule manja ake moyang'anizana ndi mapewa ake pa nthawi imene akuyamba kunena Takbir, kenako atsitse manja akewo ndi kugwira dzanja lake lamanja chikhato cha dzanja la manzere, ndipo awaike manjawo kunsi kwa chidali chake, ndipo adziyang'ana pamalo ake wochitira Sajdat. Kenako atsegule Swalaat ndi ma Du'aa ena omwe adza mu Hadith, monga kuti ***Sub- hanakAllahumma, wabihamdika watabaarakaats - muka, wata - alaa Jadduka, walailaha ghairuka***[1] Kenako anene Ta - aw - wudh, nkuwerenga Bismillah ndipo kenako awerenge Faatihat. Ndipo ndi bwino kwa munthu wotsatira kuti aiwerenge Faatihat mu Swalaat zomwe Imaam sakweza mau ndi momwe sakweza mau ngati Swalaatyo ili yokweza mau. Ndipo zili Waajib kuti Faatihat iwerengedwe mu Swalaat yosakweza mau. Kenako awerenge paliponse pomwe papepuka mu Quràn. Ndipo ndi Sunnat kuti awerenge pa Swalaat ya Fajr kuchokera m'chigawo cha Surat zitalizitali, ndipo pa Maghrib kuchokera m'chigawo cha Surat zifupizifupi, ndipo mu Swalaat zina zonse kuchokera m'chigawo cha Surat za pakatikati. Ndipo chigawo cha Surat zitalizitali chinayambira pa Surat Qaaf mpaka surat Amma, ndipo zapakatikati mpaka Surat Dhuha, ndipo zazifupi zake mpaka Surat Nass. Ndipo pa Swalaat ya Subuhi Imaam adzakweza mau powerenga, adzakwezanso mau m'marakaat awiri oyambirira a Maghrib ndi Isha, ndipo sadzakweza mau mosakhala m'marakaat amenewa. Kenako adzanena Takbir ndikuchita Ruku, ndipo adzaika manja ake m'maondo atalekanitsa zala zake ndi kuongola msana wake, ndipo adzapanga mutu wake kukhala wofanana ndi msana wake, kenako adzanena katatu mau akuti ***sub-hana Rabbiyal- Adhweem***. Kenako adzautsa mutu wake akunena kuti samiAllahu liman hamidah, ndipo akaongoka ali chiimire anene kuti Rabbana walakal- hamdu hamdan katheeran Twayyiban Mubaarakaatn feeh, mil-us-samawaati wamil-ul-ardh wamil-u- mashita min shai- in bad, kenako akunena Takbir adzapita kokachita sajdat, ndipo adzatalikitsa manja ake ndi nthiti zake, ndinso mimba yake ndi ntchafu zake. Ndipo adzaika manja pansi moyang'anizana ndi mapewa ake. ndipo nsonga za mapazi ake zikhale zitalunjika ku Qiblat, komanso zala za manja ake. Kenako anene katatu kuti sub-hana Rabbiyal- a'laa. Ndipo zili kwa iye kuwonjezera maduàa ena omwe adza mu Hadith, kapena kuti apemphe chomwe akufuna. Kenako akunena Takbirat autse mutu wake ndi kuyala

[1] (ulemelero ndi Wanu E, Mbuye wathu, ndi kutamandidwa Kwanu, ndipo ladalitsika dzina Lanu, ulemerero Wanu watukuka, ndipo palibe Mulungu wopembedzedwa mwachoonadi wosakhala Inu).

mwendo wake wamanzere naukhalira, ndipo aimike phazi lake lamanja ndi kupana zala zake molunjikitsa ku Qiblat, kapena aimike mapazi ake awiri ndipo zala zake azilunjikitse ku Qiblat nakhalira zidendene zake, ndipo anene kuti ***Rabbigh-fir-li,*** kokwanira kawiri, ndipo zili kwa iye kuonjezera mau onena kuti ***War- hamni, waj-bur-ni, war-faani war-zuq-ni, wansur-ni, wah-dini, wa-a fini,***[1] Kenako adzachita sajdat yachiwiri ngati yoyamba nautsa mutu wake akunena Takbirat, ndipo adzadzuka kuimilira ndi nsonga za mapazi ake, motero adzaswali Rakaat yachiwiri ngati yoyamba. Choncho akamaliza marakaat awiriwo adzakhala mokhalira mwendo ataika dzanja lake lamanzere pa tchafu yake ya kumanzere, ndipo dzanja la manja pa ntchafu ya manja, nafumbata ku dzanja lamanjalo kachala kakang'ono ndi kotsatizana nako, ndipo adzazunguza chala chachikulu ndi chapakati ndikulozera ndi chamkomba phala nanena kuti ATTAHIYYAATU LILLAHI WAS-SWALAATWAATU WATTWAYYIBAATU, ASSALAAMU ALAIKA AYYUHANNABIYYU WARAH MATULLAHI WABARAKAATTUH ASSALAAMU ALAINA WA ALA IBAADILLAHIS- SWAALIHEEN, ASH-HADU AN-LAA ILAAHA ILLALLAHU WA-ASH-HADU ANNA MU-HAMMADAN ABDUHU WARASULUH.[2]

Kenako adzaimiriranso mu Swalaat za marakaat atatu ndi za marakaat anayi ndikutukula manja ake akunena Takbirat, ndipo adzaswali marakaat ena otsala chimodzimodzi, koma sadzakweza mau m'marakaat amenewo, ndipo adzawerenga Faatihat yokha basi .Kenako adzakhala mokhalira thako kuti achite Tashah-hud yomaliza, adzayala mwendo wamanzere ndikuutulutsira ku manja, ndipo adzaimika phazi la manja, thako lake atakhazika pansi ndipo pa kukhala komaliza ,kumakhala mu Swalaat yomwe ili ndi ma Tashah-hud awiri kenako adzanena Tashah-hud yoyamba ndi kunenenanso mau akuti: ALLAHUMMA SWALLI ALA MUHAMMAD WA ALAA AALI MUHAMMAD , KAMA SWALLAITA ALAA IBRAHIM WA ALAA AALI IBRAHIM , INNAKA HAMEEDDUM'MAJEED , ALLAHUMMA , BAARIK ALA MUHAMMAD WA ALAA AALI MUHAMMAD ,KAMAA BAARAKTA ALAA IBRAAHIM WA ALAA AALI IBRAAHIM , INNAKA HAMEED UM'MAJEED."[3]

Ndipo ndi Sunnat kunena kuti ***Audhu billahi min adhaabinnar wa adhaabilqabr, wafinatil mahya wal mamaat, wafit- natil maseeh dajjaal.***[4]

---

[1] (E, Mbuye wanga ndikhululukireni, ndimvereni chisoni, lumikizani Niyyat yanga, nditukuleni, ndipatseni rizq).

[2] (Ulemu onse oyankhula, Swalaat zonse ndi zabwino zonse ndi za Allah , mtendere ukhale pa iwe oh , Mneneri, chifundo cha Allah komanso madalitso Ake, mtendere ukhale pa ife ndi pa akapolo a Allah ochita zabwino, ndikuikira umboni kuti palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma Allah, ndikuikiranso umboni kuti Muhammad ndi kapolo wa Allah komanso ndi Mtumiki Wake).

[3] (E, Allah! Tumizani chifundo kwa Muhammad ndi ku banja la Muhammad, monga m'mene munatumizira chifundo kwa Ibrahim ndi ku banja la Ibrahim , ndithu Ndinu Wotamandidwa, Wolemekezeka. Ndipo tumizani madalitso kwa Muhammad ndi ku banja la Muhammad monga m'mene munatumizira madalitso kwa Ibrahim ndi ku banja la Ibrahim ndithu Ndinu Wotamandidwa Wolemekezeka).

[4] Kutanthauza kuti ndikudzitchinjiriza mwa Allah ku chilango cha moto, cha m'manda, kumayesero a maseeh dajjaal.

Ndinso ma duàa ena omwe adza mu Hadith. Kenako apereke salaam ziwiri choncho adzacheukira ku manja akunene kuti Assalaamu alaykum warahmatullah. Kenako kumanzere, pambuyo pake ndi sunnatnso kunena Duàa yomwe yadza mu Hadith;[1]

## SWALAAT YA MUNTHU WODWALA

Zikakhala kuti kuimirira kukuonjezera matenda ake, kapena sangathe kuimirira aswali chikhalire, ngati sangathe kukhala aswali atagona cham'mbali, ngati zingam'vute kuswali atagona cham'mbali aswali atagona chagada, ndipo ngati atalephera kuchita Ruku ndi Sajdat adzangochita molozera, ndipo adzafunika kubweza Swalaat zomwe zamudutsa. Ndipo ngati zitamuvuta iye kuswali Swalaat iliyonse mu nthawi yake, zili kwa iye kuphatikiza Zuhr ndi Asr, komanso Maghrib ndi Isha pa nthawi imodzi mu nthawi ya imodzi ya Swalaat ziwirizi.

## SWALAAT YA MUNTHU WA PAULENDO

Ngati mtunda wa ulendo wake ndiwotalika kupitirira pafupifupi ma kilomita makumi asanu ndi mphambu zitatu (85 km) ndipo ulendo wakewo ndi wololedwa, ndiye kuti akuloledwa kupungula marakaat awiri Swalaat ya marakaat anayi (4). Ndipo ngati atachita Niyyat kuti akhala pa malo ena ake mkatikati mwa ulendo wake masiku opitirira anayi, (swalaat za fardhwi 20) ndiye kuti iye adzakwaniritsa marakaath onse kuchokera tsiku limene wafika ndipo sapungula. Ngati munthu wapaulendo waswali pambuyo pa Imaam amene sali paulendo, kapena anayiwala Swalaat imene inam'dutsa asananyamuke ulendo ndipo waikumbukira ali pa ulendo, kapena anaiwala Swalaat imene inam'dutsa ali paulendo ndipo waikumbukira atamaliza ulendo ndiye kuti Swalaat zonse zanenedwazi

---

[1] yomwe ndiyoti :As-tagh- firullah (katatu), Allahumma Antassalaam waminkasalaam, Tabarakta ya Dhal-Jalaali wal-Ikraam, Laa ilaaha illAllahu wah-dahu la sharika lah, lahul-Mulk walahul hamdu wahuwa ala kullishai-in Qadeer, La haula wala quw- wata illa billah, Laa ilaaha illAllahu wala nàbudu illa Iyyaahu, Lahunnimat walahul fadh-lu walahuth-thana-ul-hasan, Laa ilaaha illAllahu mukh-lisweena lahud-deena walau karihal kaafiroon, Allahumma la maania lima a' twaita, wala lima mana'ta wala yan-fau' dhal jaddi minkal- jaddu.Anenenso pambuyo pa Swalaat ya fajr ndi ya Maghrib pamodzi ndi ma Duàa amene anenedwa kalewa kuti Laa ilaaha illAllahu wah-dahu la sharika LAHU, LAHUL-Mulku walahul- hamdu, yuhyi wayumeetu , wahuwa ala kullishai-in Qadeer (Kakhumi),
(E, Allah! Ndinu mtendere, ndipo kwa Inu kumachokera mtendere, mwadalitsika e, Inu mwini ulemerero ndi kupatsa, palibe wopembedzedwa mwachonadi koma Allah yekhayo alibe wothandizana Naye. Ufumu ndi kutamandidwa konse ndi Zake , ndipo Iye ndi wamphamvu pa chilichonse. Palibe nzeru yosiyira zoipa ngakhale mphamvu zochitira zabwino koma zonse zili m'manja mwa Allah, palibe wopembedzedwa mwachoonadi koma Allah ndipo palibe amene timampembedza koma Iyeyo. Mtendere , ubwino ndi kuyamikiridwa kwabwino ndi Zake, palibe wopembedzedwa mwachoonadi koma Allah momuyeretsera chipembedzo ngakhale ataipidwa nazo makafiri, E, Allah! Palibe angatsekereze chimene mwapereka, ndipo palibe angapereke chomwe inu mwatsekereza ndipo ubwana sungathandize mwini ubwana ku chilango chochokera kwa Inu). Ndipo pambuyo pa Swalaat ya Fajr ndi Maghrib pamodzi ndi zomwe zanenedwa anene kuti. Palibe wopembedzedwa mwachoonadi koma Allah Yekhayo, Alibe wothandizana Naye, ufumu ndi kutamandidwa konse ndi Zake, Amapereka moyo ndi imfa, ndipo Iye ndi Wamphamvu pa chilichonse Pambuyo pa zimenezo. Kenako anene kuti ***Sub - hanAllah***, ka (33) ***Wal - hamdu lillah***, ka (33) ***WAllahu Akbar,*** ka (33) ndipo pokwaniritsa ka (100) anene kuti Laa illah illAllahu wah-dahu la sharika lah, lahul mulku walahul hamdu, wahuwa ala kulli Shai -in Qadeer. Kenako awerenge Ayatul kursi, kenako n'kudzawerenga ikhlas, Falaq ndi Naas, ndipo adzabwerezabwereza kuwerenga surat izi: Ikhlaas, Falaq ndi Nass pambuyo pa Swalaat ziwiri Fajr ndi Maghrib katatukatatu.

adzakwaniritsa sadzapungula. Ndipo wapaulendo akuloledwa kukwaniritsa marakaat onse, koma kupungula ndibwino kwambiri.

**SWALAAT YA JUMUAT**

Ndipo iyo ili ndi ulemelero waukulu kuposa Zuhr, ndiponso ndi Swalaat yapadera, sikuti yachita kupungulidwa Swalaat ya Zuhr. Choncho sikuloledwa kuiswali marakaat anayi, ndipo siingatheke ndi Niyyat ya Zuhr, ndiponso sizikuloledwa kuiphatikiza ndi Swalaat ya Asr ngakhale chitapezeka chifukwa chophatikizira.

**SWALAAT YA WITR**

Ndi Sunnat, ndipo nthawi yake, ndi kuyambira pambuyo pa Swalaat ya Isha kufikira kutuluka kwa m'bandakucha. Ndipo kuchepa kwa marakaat ake,ndi Rakaat imodzi, ndipo kuchuluka kwake ndi marakaat khumi ndi imodzi, kupereka Salaam pambuyo pa marakaat awiri alionse ndibwino kwambiri. Ndipo zili sunnat kuwerenga Suuratul Aalaa mu rakaat yoyamba, Al Kaafiruun mu yachiwiri ndi Al Ikhlaas mu yachitatu. Zili sunnat kuchita Qunuut pambuyo pa rukuu ndipo atukule manja ake n'kuchita duwa mokweza mawu angakhale atakhala yekha.

**MALIRO**

Kusambitsa maliro a Msilamu, kuwaveka sanda, kuwaswalira, kuwanyamula kupita nawo kumanda ndi kuwakumbulira m'manda, zonsezi zili Fardh kifaayat; kupatula yemwe wafera ku nkhondo ya chipembedzo, pakuti iye sasambitsidwa ndiponso savekedwa sanda, koma zikuloledwa kumuswalira, ndiponso aikidwe m'manda m'mene analiri pa nthawi yomwe amamwalira. Ndipo mwamuna avekedwe nsalu zoyera zitatu, ndipo wamkazi avekedwe nsalu zisanu: Chilundu, mpango, malaya ndi nsalu ziwiri. Ndipo ndi Sunnat kuimirira Imaam komanso woswalira payekha pafupi ndi pachidali cha mtembo wachimuna ndi kuima pakati pa mtembo wachikazi, choncho adzanena ma Takbirat anayi akutukula manja ake pa Takbirat iliyonse, adzayamba Takbirat yoyamba ndipo adzawerenga Ta -aw - wudh komanso Tasmiyat ndikuwerenga Faatihat yokha mwachinsinsi, kenako adzanena Takbirat yachiwiri ndikunena Swaliyatume, kenako adzanena Takbirat yachitatu ndikuwachitira duàa maliro, kenako adzanena Takbirat yachinayi ndikuima pang'ono, kenako nkupereka Salaam. Ndipo zili Haraam kukweza mtumbira wa manda kopitirira mkono umodzi, kuwamangira chiliza ndi kuwapsopsona, kuwafukitsira ubani ndi kulemba kapena kukhala kapena kuponda pa mandapo. Ndipo zili haraam kuyatsa nyale pa manda, ku wachita TWAWAAF, kumangapo mzikiti kapena kukumbulira mu mzikiti.

Ndipo zili waajib kugumula nyumba zomwe zamangidwa pa mandapo.

- Palibe mau enieni a chipepeso, ndipo ena mwa iwo, wopepesayo anene kuti A'adhwamAllahu ajraka, wa ah - sana aza - aka, waghafara limayyitika.(Allah akulitse malipiro ako, achichite chipepeso chako kukhala chabwino ndipo awakhululukire maliro ako). Ndipo chipepeso cha Msilamu kwa kafiri anene kuti A'dhwamAllahu ajraka, wa ah - sana azaaka. Ndipo chipepeso cha kafiri n'chosaloledwa ngakhale wopepesedwayo ali Msilamu.
- Zili Waajib kwa amene wazindikira kuti a m'banja lake adzakhala akumulilira motamanda zabwino zake akadzamwalira kuti awauze kuti asadzalire motero, ndipo akapanda kuwauza adzalangidwa chifukwa cha kulira kwao komulilira iye.

- Imaam Shafi (RA) ananena kuti sibwino kukhala pa malo kudikirira chipepeso, komwe ndi kusonkhana kwa anamalira m’nyumba ina yake kuti aziwapeza amene akufuna kudzapepesa, koma ziyenera kuti abalalikane ku zintchito zawo, amuna ngakhalenso akazi.
- Ndi Sunnat kuwapangira chakudya anamalira ndipo sibwino kuwadyera chakudya, kapena kuwaphikira chakudya amene asonkhana pamasiyepo.
- Ndi Sunnat kukaona manda a Msilamu mosachita kumangira ulendo, zikuloledwanso kukaona manda a kafiri, ndiponso kafiri asaletsedwe kukaona manda a Msilamu.
- Ndi Sunnat kwa amene walowa ku manda kunena kuti: Assalaamu Alaykum daaraqaumin mu'mineen, wa inna insha Allah bikum lalaahiqoon, yar - hamullahul - mustaqdimeena wal - mustakhireen, Nas - alullaha lana Walakumul - aafiyyah, Allahumma la tah - rimna ajrahum, wala taf - tin'na ba'dahum waghfir lana walahum.

(Mtendere ukhale kwa inu eni, nyumba amanda amene muli okhulupirira - kapena kuti: eni nyumba mwa amene ali okhulupirira-ndipo ife Allah akalola tidzakumana nanu, Allah awachitire chifundo amene anatsogola mwa ife ndi amene amalizira, tikum’pempha Allah kuti atipatse ife ndi inu mpumulo wabwino, E, Allah! Musatimane malipiro awo, ndipo musatipatse mayesero m'mbuyo mwawo, ndipo tikhululukireni ife ndi iwo).

**SWALAAT YA EID ZIWIRI:** Iyo ndi Fardh kifaayat, ndipo nthawi yake ili ngati nthawi ya Swalaat ya Dhuhaa, choncho ngati zitadziwika kuti linali tsiku la Eid dzuwa litapendekeka, ndiye kuti idzaswalidwa mawa lake kukhala Qadhwaa. Ndipo zofunikira zake zili ngati zofunikira za Swalaat ya Jumuat kupatula ma Khutbat awiri, ndipo ndi makrooh kuswali Nafl isanaswalidwe kapena itsaswalidwa pabwalo loswalira Eid. Ndipo kaswalidwe kake ndi aka: akhale marakaat awiri; atanena Takbeera ya Ihram yoyamba asananene Ta'aw - wadh adzanena ma Takbeera asanu ndi imodzi mu Rakaat yoyamba, ndipo mu Rakaat yachiwiri adzanena ma Takbeera asanu asanayambe kuwerenga Quran, ndipo adzatukula manja ake awiri ponena Takbeera iliyonse. Kenako anene Ta'aw'wudh ndi kuwerenga Surat Faatihat mokweza mau kenako awerenge Surat A'laa mu Rakaat yoyambirira, ndikuwerenga surat Ghashiyah mu Rakaat yachiwiri. Choncho akapereka Salaam adzapanga ma khutbat awiri ngati ma khutbat awiri a Jumuat; koma zili Sunnat kuti achulutse kunena ma Takbeera m'ma khutbat awiriwo, ndipo ngati ataswali Eid ngati Nafl palibe vuto chifukwa choti ma Takbeera owonjezera ndi Zikr zomwe zimakhala pakati pa marakaat awiri zili Sunnat.

**SWALAAT YA KADANSANA:** Ndipo iyo ili Sunnat, ndipo nthawi yake ndi kuyambira pamene kadansana wachitika kapena kufooka kwa kuwala kwa mwezi mpaka atachoka. Ndipo Swalaat imeneyi singachitidwe Qadhwaa ngati chitachoka chifukwa chake. Ndipo iyo imaswalidwa marakaat awiri, mu Rakaat yoyambirira adzawerenga Surat Faatihat ndi Surat ina yaitali mokweza mau, kenako adzachita Ruku yaitali; kenako adzaweramuka ndikunena mau oti samiAllahu ndi mau oti Rabbana walakal hamdu. Ndipo sadzapita pa sajdat koma adzawerenga Faatihat ndi

Surat yaitali, kenako adzachita Ruku yaitali, kenako adzaweramuka ndikuchita Sajdat ziwiri zazitali, kenako adzaswali Rakaat yachiwiri ngati yoyambirira, kenako adzachita Tashahhud ndi kupereka Salaamu. Ndipo wotsatira akabwera pambuyo pa Ruku yoyamba ndiye kuti sanaipeze Rakaat.

**SWALAAT YOPEMPHERA MVULA:** Kukachitika chilala ndikuchepa mvula, zili Sunnat kuswali Swalaat imeneyi. Ndipo nthawi yake, kaswalidwe kake ndi malamulo ake zili ngati Swalaat ya Eid, kungoti pa Swalaat imeneyi adzawapangira anthuwo Khutbah imodzi kutha kwa Swalaatyo. Ndipo zili Sunnat kutembenuza nsalu kumapeto kwa Swalaatyo, kutengera pofuna kutembenuza nyengo momwe ilili.

**SWALAAT ZA NAFL: Z**atsimikizika kuti Mtumiki (SAW) amaswali tsiku lili lonse pambali pa Swalaat za faradhwi marakaat khumi ndi awiri (12) motere: Rakaat ziwiri asadaswali Al Fajr, marakaat anayi asadaswali Zuhr, Rakaat ziwiri pambuyo pake, rakaat ziwiri pambuyo pa Maghrib ndi ziwiri pambuyo pa Ishaa. Komanso kwalandiridwa ma hadith ena kuchokera kwa Iye (SAW) kutinso ankaswalinso Swalaat zina za nafl pambali pa izi.

**NTHAWI ZOLETSEDWA KUSWALI:** Ndi haraam kuswali Swalaat za sunnat kapena zina mwa izo mu nthawi zimene kuletsa kwatsimikizika kuswali mu nthawizo. Zimenezi ndi izi **(1)** kuchokera kutuluka kwa m'bandakucha (pambuyo poswali Swalaat ya Al Fajr kufikira kutuluka kwa dzuwa ndikukwera kwa mlingo wa mkondo). **(2)** Nthawi yoti dzuwa lili paliombo kufikira litapendekeka. **(3)** Kuchokera pambuyo pa Swalaat ya Asr kufikira dzuwa litalowa. Tsono Swalaat zomwe zili ndi zifukwa zake ndiye zikuvomerezeka kuziswali mu nthawi zimenezi monga tahiyyatul –Masjid, rakaat ziwiri zoswalira chifukwa cha Twawaaf, sunnat ya Alfajr, Swalaat ya Janaazat, rakaat ziwiri za udhu, sajdat ya Tilaawat komanso ya shukr (yothokoza Allah).

**MALAMULO A MIZIKITI**: Ndiyofunika kuimanga m'mene ingafunikire, ndipo mizikitiyo ndi mabwalo okondedwa kwambiri kwa Allah. Ndipo ndi Haraam kuimbiramo nyimbo (zosangalatsa) komanso kuomba m'manja, kuimba zing'wenyeng'wenye, kulakatula ndakatulo za Haraam, kusakanikirana amuna ndi akazi, kugonana, kugulitsa komanso kugula, ndipo ndi Sunnat kumuuza wogulitsayo kuti Allah asapindulitse malonda ako, zilinso Haraam kufunsa chinthu chotaika, ndi Sunnatnso kwa amene wamumva wofunsayo kunena kuti Allah asakubwezere chotaikacho.

Ndipo zikuloledwa kuwaphunzitsiramo ana amene sakupereka vuto, kumangitsa ukwati, kugamula mulandu, kulakatula ndakatulo zololedwa, kugonamo kwa amene ali pa Itikaaf ndi amene sali pa Itikaaf, kugona mlendo, wodwala komanso tulo ta masana.

Ndipo ndi Sunnat kuiteteza posachitamo phokoso, kukangana, kuchulutsa kuchezamo, kukweza mau ndi zinthu zosakhala bwino ndi kuisandutsa njira popanda chifukwa.

Ndipo sibwino kukambamo nkhani zopanda pake pa zinthu za duniya, ndipo isagwiritsidwe ntchito miswala yake kapena nyale zake, kapena magetsi ochokera m'mizikitimo mmalo onga chikwati ndi chipepeso.

# ZAKAAT

**Mitundu ya zinthu zoperekera Zakaat. Zakaat ili Waajib m'mitundu ya zinthu zinayi: Mtundu woyamba:** Zifuyo. **Wachiwiri:** Chotuluka kuchokera mu nthaka. **Wachitatu:** Golide ndi Siliva. **Wachinayi:** Katundu wa malonda.

**ZOFUNIKIRA KUTI ZAKAAT IKHALE WAAJIB**

**Ndipo Zakaat singakhale Waajib pokhapokha patapezeka zofunikira zisanu:**
**Choyamba**: Woperekayo akhale Msilamu. **Chachiwiri**: Woperekayo akhale mfulu. **Chachitatu**: Chumacho chikwanire mlingo woperekera Zakaat. **Chachinayi**: Pakhale umwini wokwanira pa chumacho. **Chachisanu**: Chumacho chikhale chilipo kokwanira chaka chatunthu kupatula chinthu chotuluka kuchokera m'nthaka.

**ZAKAAT YA ZIFUYO:** Ndipo izo zili m'mitundu itatu: Ngamira, ng'ombe ndi mbuzi kapena nkhosa. Ndipo kuti Zakaat ikhale Waajib pa zifuyo zimenezi payenera kupezeka zofunikira ziwiri: **1)** Zibusidwe kwa chaka kapena kuposera apo **2)** Zikhale za mkaka ndi mbeu, osati zogwirira ntchito. Tsopano zikakhala za malonda Zakaat yake idzakhala Zakaat ya katundu wa malonda.

## ZAKAAT YA NGAMIRA ILI CHONCHI :

| **Chiwerengero** | **1 - 4** | **5 - 9** | **10 - 14** | **15 - 19** | **20 - 24** | **25 - 35** | **36 - 45** | **46 - 60** | **61 - 75** | **76 - 90** | **91- 120** |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| **Zakaat yake** | Osapereka Zakaat | Mbuzi imodzi | Mbuzi ziwiri | Mbuzi zitatu | Mbuzi zinayi | Ngamira yomwe yalowa m'chaka choyamba. | Ngamira ya zaka ziwiri | ngamira ya zaka zitatu | ngamira ya zaka zinayi | ngamira ziwiri zazikazi za zaka ziwiri | Misoti ya ngamira iwiri ya zaka zitatu |
| Choncho zikaonjezereka pa ngamira (120) adzapereka pa ngamira makumi asanu zili zonse adzapereka msoti wa zaka ziwiri. | | | | | | | | | | | |

## ZAKAAT YA NG'OMBE ILI CHONCHI :

| **Chiwerengero** | **1-29** | **30-39** | **40-59** |
|---|---|---|---|
| **Zakaat yake** | Osapereka Zakaat | Ng'ombe ya tonde kapena yaikazi ya chaka chimodzi | Tonde kapena yaikazi ya zaka ziwiri |
| Choncho ng'ombe zikakwana makumi asanu ndi imodzi(60) kapena kupitirira apo, ndiye kuti pa ng'ombe makumi atatu zilizonse adzapereka katonde ka chaka chimodzi. Ndipo pa ng'ombe makumi anayi zilizonse adzapereka msoti wa zaka ziwiri. | | | |

## ZAKAAT YA MBUZI ILI CHONCHI :

| **Chiwerengero** | **1-39** | **40-120** | **121-200** | **201-399** |
|---|---|---|---|---|
| **Zakaat yake** | Osapereka zakaat | Mbuzi imodzi | Mbuzi ziwiri | Mbuzi zitatu |
| Choncho zikakwanira mazana anayi (400) kapena kupitirira apo ndiye kuti pa mbuzi zana limodzi lililonse adzapereka mbuzi imodzi. Mu Zakaat ya mbuzi asaperekedwe tonde ngakhale yokalamba, ngakhale yopunduka diso kapena yaikazi imene ikulera mwana wake, kapenanso yomwe ili ndi bere, ngakhalenso yodula kwambiri. Mbuzi yaikazi msinkhu wake chaka chimodzi pamene nkhosa ndi imene yakwana miyezi isanu ndi umodzi (6). | | | | |

**ZAKAAT YA (MBEU) ZOTULUKA MNTHAKA:** Zakaat ili Waajib mu zomera zilizonse za mbeu ndi zipatso ngati patapezeka zofunikira zitatu.

**1.** Mbeuzo zikhale mu zomwe zimayezedwa ndi chiwiya ndiponso zimasungidwa; monga mchewere ndi tirigu kuchokera m'mbeu, komanso monga mphesa ndi tende kuchokera m'zipatso. Koma zomwe siziyezedwa ndi chiwiya monga ndiwo zamasamba ndi zina zotero zilibe kupereka Zakaat.

**2.** Kukwanira mlingo woperekera Zakaat womwe ndi makilogaramu okwanira (653) kapena kupitirira apo.

**3.** Zomerazo zikhale zili m'manja mwke pa nthawi yofunika kupereka Zakaat. Ndipo nthawi yofunika Zakaat ndi kuonekera kwa kukhwima kwa zipatso (pa kufira kapena kuoneka chikasu), ndipo mbeu chifukwa cha kukhwima ndi kuuma kwake .

Ndipo zidzafunika kupereka (10%) mu zomwe zathiriridwa mosavutikira monga zomwe zathiriridwa ndi mvula komanso mitsinje. Ndipo adzapereka theka la chakhumi (5%) mu zomwe zathiriridwa movutikira, monga madzi otungidwa kuchokera mu zitsime ndi ena otero.Tsopano zomwe zathiriridwa movutikira m'masiku ena a pa chaka ndiponso mosavutikira m'masiku otsala a pa chaka, zimenezo zidzaoneka molingana ndi zawirikiza mwa ziwirizo, ndipo chiwerengero chidzakhala molingana ndi masiku ovutikira ndi mosavutikira.

**ZAKAAT YA ZINTHU ZIWIRI ZA MTENGO WAPATALI**

**Zinthu ziwiri za mtengo wapatali zili pawiri:**

**1.** Golide, palibe kupereka Zakaat mpaka itakwanira kulemera kwake 85 gms.

**2.** Siliva, palibe kupereka Zakaat pa siliva mpaka itakwana 595gms,. Ndipo pa ndalama za chitsulo ndi za pepala (zomwe zikugwira ntchito palibe kupereka Zakaat) mpaka zitakwanira mtengo wake pa nthawi yopereka Zakaat womwe ndi wosachepera mlingo wa golide ndi siliva . Mlingo wa kuperekera Zakaat ya golide ndi siliva ndi 2.5% .

Zodzikongoletsera za golide zomwe zili zololedwa zomwe zinaikidwa kuti ndizogwiritsira ntchito, palibe kuziperekera Zakaat, koma zomwe zinaikidwa kuti n'zobwereketsa n'kumalandirira ndalama .kapena kungozisunga zimenezo n'zofunika kuziperekera Zakaat.

Ndipo zikuloledwa kwa amayi chilichonse chomwe adazolowera kuchivala kuchokera mu golide ndi siliva, ndipo zikuloledwa kwa amuna kuvala siliva wochepa osasakaniza ndi kena kalikonse monga mphete ya siliva, magalasi a m'maso ndi zina zotero.Tsono golide ndiyosaloledwa kuika kalikonse pachiwiya, ndipo zikuloledwa kwa amuna kugwiritsa ntchito golide wochepa wotsatira pa china chake, monga batani pa chovala , ndi kumangira dzino mosadzifananiza ndi akazi.

Ndipo amene ali ndi chuma chomwe chimakwera ndi kutsika, ndipo chimamvuta iye kuperekera Zakaat gawo lililonse la chumacho pakatha chaka ndiye kuti adzachiperekera Zakaat pa tsiku lomwe adzalikhazikitse pa chaka, ndipo pa tsiku limenelo adzaona kuti ali ndi chuma chochuluka bwanji? Choncho adzachiperekera 2.5% ngakhale kuti china mwa chuma chake sichinakwanitse chaka, ndipo munthu amene amalandira ndalama , kapena ali ndi chinthu chobwereketsa n'kumalandira ndalama monga nyumba ndi malo, ngati sakusunga

ndalama iliyonse mu zimenezo palibe kupereka Zakaat ngakhale zitachuluka. Koma ngati akusungaira mu ndalamazo adzapereka Zakaat zomwe anasungira patadutsa chaka. Koma ngati zitam'vuta iye kaperekedwe kake adzasankha tsiku loperekera Zakaat pa chaka monga zanenedwa kale .

**ZAKAAT YA NGONGOLE:** Amene ali ndi ngongole imene ili m'mnja mwa munthu wolemera, kapena ali ndi chuma chomwe angathe kuchipulumutsa ayenera kuchiperekera Zakaat akachilandira chifukwa cha kuchuluka kwa zaka ngakhale zitachuluka, koma ngati chili chovuta kuchipulumutsa, monga ngongole yomwe ili m'manja mwa munthu amene chuma chake chinatha sangaiperekere Zakaat chifukwa choti iye sangathe kuigwiritsa ntchito.

**ZAKAAT YA KATUNDU WA MALONDA**

Katundu wa malonda sangaperekere Zakaat pokhapokha patapezeka zofunikira zinayi: **1.** Katunduyo akhale wake. **2.** Achite Niyyat yoti katunduyo ndi wamalonda. **3.** Mtengo wa katunduyo ukwanire mlimgo wa Zakaat, womwe ndi mtengo wochepetsetsa wa mlingo wa golide kapena siliva. **4.** Katunduyo akwanitse chaka.
Ndiye zofunikira zimenezi zikapezeka adzapereka Zakaat kuchokera mu ndalama za katunduyo , ndipo ngati anali ndi golide kapena siliva , kapena ndalama , ndiye kuti adzaziphatikiza ndi ndalama zomwe zili m'katundu wa malonda pofuna kukwaniritsa mlingo woperekera Zakaat . Ndipo akachita Niyyat ya kugwiritsa ntchito pa nyumba katundu wa malonda monga nsalu, nyumba, galimoto ndi zina zotero, ndiye kuti katundu ameneyo sadzaperekera Zakaat, kenako ngati pambuyo pake n'kuchita Niyyat ya malonda katunduyo, ndiye kuti adzayambiranso atakwanira chaka.

**ZAKAAT YA FITR:** Zakaat ya Fitr ili waajib kwa Msilamu aliyense, akakhala ndi chuma choonjezera pa chakudya chake ndi chakudya cha anthu ake amene amawasamalira mu usiku woti mawa ndi Eid , ndinso chakudya choti angadye pa tsiku la Eid .Ndipo mlingo wake ; ndi makilo awiri ndi theka(2½ Kgs) a chakudya chomwe anthu a dziko limenelo amadalira, kwa munthu mmodzi aliyense wamwamuna kapena wamkazi Ndipo amene wafunika kuipereka Zakaat'yo am'perekerenso amene amam'samalira mu usiku woti mawa ndi Eid ngati Zakaat'yo alinayo. Ndipo zili bwino kuipereka tsiku la Eid , asanaswali Eid . Ndipo sizikuloledwa kuichedwetsa mpaka kumaliza kuswali Eid, koma zikuloledwa kuiperekeratu patatsala masiku awiri kapena limodzi kuti tsiku la Eid lifike. Ndipo zikuloledwa kuti munthu mmodzi apatsidwe zomwe zinafunika kupatsidwa gulu, ndi kupatsidwa gulu zomwe zinafunika kupatsidwa munthu mmodzi.

**KUPEREKA ZAKAAT**: Zili waajib kupereka Zakaat mwachangu, ndipo m'yang'aniri wa mwana ndi munthu wamisala ayenera kuwaperekera Zakaat awiriwo. Ndipo zili Sunnat kuionetsera Zakaat'yo ndikuti mwini wake zakaat'yo aigawe yekha. Ndipo nzofunikira popereka Zakaat'yo pakhale Niyyat kwa munthu wamkulu, ndipo sizingakwanire kuti wapereka Zakaat ngati amachita Niyyat ya sadaka wamba ngakhale atapereka sadaka ndi chuma chake chonse. Ndipo ndibwino kwambiri kuiyika zakaat ya chuma chilichonse mwa anthu osauka a m'dziko lakelo. Ndipo zikuloledwa kuitenga kupita nayo ku dziko lina, ngati

zitafunikira kutero. Ndipo n'zotheka kuperekeratu Zakaat ya zaka ziwiri ngati mlingo utakwanira.

**OLANDIRA ZAKAAT: Ndipo iwo alipo asanu ndi atatu:**
(1) Anthu osowa (2) Anthu osauka (3) Anthu amene akugwira ntchito yosonkhanitsa Zakaat (4) Anthu owalimbikitsa mitima yawo pa Chisilamu (5) Akapolo ndi Akaidi (6) Amene ali ndi ngongole (7) Amene ali pa njira ya Allah (8) Munthu wapaulendo.
Choncho onsewa adzapatsidwa zakaat molingana ndi kuvutika kwawo, kupatula amene akugwira ntchito ya Zakaat'yo iwo adzapatsidwa molingana ndi malipiro ake ngakhale atakhala olemera. Ndipo n'zotheka kuipereka zakaat kwa anthu oukira ndi zigawenga ngati dziko limene wopereka Zakaatyo lili m'manja mwa iwo, ndiponso zikukwanira kuti wapereka zakaat ngati mtsogoleri waitenga mokakamiza kapena mwa kufuna kwa munthu woperekayo, wachita nayo chilungamo kapena wapondereza.

N'zosatheka kuipereka Zakaat kwa kafiri, kapena kapolo (amene sanapatsidwe ufulu wodziombola). Wolemera, amene ali wofunika kudyetsedwa ndi munthu amene akupereka Zakaat'yo, ndi a banja la Hashim. Choncho ngati atapereka Zakaat kwa munthu osayenerera mosadziwa kenako nkudziwa ndiye kuti sinamthekere, kupatula ngati ataipereka kwa munthu amene amamuganizira kuti ndi wosowa n'kudziwika kuti ndi wolemera ndiye kuti zakaat imeneyo yatheka.

**SADAKA YA KUFUNA KWA MUNTHU**

Mtumiki wa Allah (SAW) anati "*Ndithu mwa zomwe zidzampeze munthu wokhulupirira mu ntchito zake ndi zabwino zake atamwalira, ndi Ilm yomwe anaphunzitsa ndi kuifalitsa, mwana wabwino yemwe anamusiya, msahafu womwe anausiya m'manja mwa anthu ena, kapena mzikiti womwe anamanga, kapena nyumba ya alendo yomwe anamanga, kapena mtsinje womwe anakumba, kapena sadaka yomwe anaipereka kuchokera mu chuma chake ali wamoyo ndipo wathanzi, sawabu zake zidzampeza iye atamwalira*. **(Ibn Maajat).**

# SWAUM (KUSALA)

Zili waajib kumanga m'mwezi wa Ramadhan kwa Msilamu wa nzeru zake, wotha msinkhu, amene ali ndi kuthekera komanga, kupatula wamkazi amene ali ndi Hidhwi ndi Nifaas. Ndipo mwana alamulidwe kumanga ngati angathe kuti aizolowere.

**Ndipo kulowa kwa mwezi wa Ramadhan kumadziwika ndi chimodzi mwa zinthu ziwiri:**

**1.** Kuchiona chithunzi cha mwezi wa Ramadhan ndi umboni wa Msilamu wachilungamo wamkulu ngakhale atakhala wamkazi.

**2.** Kukwanira mwezi wa Shaabaan masiku makumi atatu (30).

Ndipo waajib yake kumayambika kutuluka kwa m'bandakucha woona mpaka kulowa kwa dzuwa. Ndipo n'koyenera kuchita Niyyat pa Swaum ya Fardh m'bandakucha usanatuluke.

## ZOMWE ZIMAONONGA SWAUM

**1.** Kugonana: Ndipo amene wachita zimenezo ayenera kumanga tsiku limenelo ndi kulipira, ndipo kulipira kwake: amasule kapolo, choncho ngati sanam'peze kapolo, ndiye kuti amange miyezi iwiri yotsatizana, ndipo amene sangathe kumanga awadyetse anthu osauka makumi asanu ndi limodzi , ndipo amene sanapeze chakudyacho palibe chimene angachite.

**2** Kutulutsa umuna: chifukwa cha kupsopsona , kapena kumukhudza wamkazi, kapena kudzitulutsa umuna, ndipo palibe vuto kwa munthu wodzilotera.

**3.** Kudya ndi kumwa mwadala, choncho ngati kuli moiwala, ndiye kuti Swaum yake ili bwino.

**4.** Kutulutsa magazi ndi kudula litsipa, kapena kupereka magazi, koma kupereka magazi ochepa kuti akayesedwe, kapena amene atuluka mosafuna, ngati otuluka pa bala ndi kamfuno, amenewo saononga Swaum.

**5.** Kudzisanzitsa. .

Ndipo ngati fumbi laulukizira kum'mero, kapena wachukucha mkamwa, kapena kuthira madzi m'mphuno ndipo madzi akafika ku m'mero, kapena waganiza zogonana umuna n'kutuluka,kapena wadzilotera, kapena magazi atuluka kuchoka mwa iye, kapena masanzi mosafuna iye ndiye kuti Swaum yake singaonongeke.

Ndipo amene wadya akuganiza kuti ndi usiku n'kutulukira kuti ndi masana, zikukakamizidwa kwa iye kuchita qaadha. Amene wadya usiku mokaikira kutuluka kwa m'bandakucha, kumanga kwakeko sikudaonongeke. Ngati wadya masana akukaikira zolowa dzuwa akakamizidwa kuchita qaadha tsiku limenelo.

## MALAMULO A AMENE SAMANGA

Zili Haraam kusamanga m'mwezi wa Ramadhan kwa amene alibe chifukwa chovomerezeka. Ndipo zili waajib kumasula kwa mkazi amene ali kumwezi, amene ali ndi Nifaas ndi munthu amene akufuna kumasula pofuna kum'pulumutsa wosalakwa ku chionongeko. Ndipo zili Sunnat kusamanga kwa munthu wapaulendo womwe iye akuloledwa kupungula marakaat a Swalaat, ngati Swaum'yo ingapereke vuto kwa iye, komanso kwa munthu wodwala amene akuopa vuto. Ndipo zikuloledwa kumasula kwa munthu amene ali pa mudzi yemwe wanyamuka ulendo mkatikati mwa usana, kwa mayi woyembekezera ndi

woyamwitsa amene akudziopera, kapena akumuopera mwana, kwa onsewa zili waajib kungobweza Swaum basi. Ndipo mayi woyembekezera ndi woyamwitsa awonjezere pa kubwezako kumudyetsa munthu wosauka pa tsiku lililonse ngati akungomuwopera mwana yekha basi.
Ndipo amene walephera kumanga chifukwa cha ukalamba, kapena matenda wosayembekezereka kuchira, pa tsiku lililonse adzamudyetsa munthu wosauka, ndipo palibe kubweza kwa iye.
Ndipo amene wachedwetsa kuchita Qadhwa pachifukwa china chake mpaka kum'peza mwezi wina wa Ramadhan adzangofunika kungochita Qadhwa basi, ndipo ngati sanachite Qadhwa mopanda chifukwa ndiye kuti pa tsiku lililonse akamachita Qadhwa adzamudyetsa munthu wosauka. Ndipo ngati wasiya kuchita Qadhwa pa chifukwa china chake namwalira palibe chomuchitira, ndipo ngati anasiya kuchita Qadhwa popanda chifukwa ndiye kuti pa tsiku lililonse lomwe sanamange adzadyetseredwa munthu wosauka. Ndipo zili Sunnat kwa m'bale wake kumanga masiku omwe sadamange obweza Swaum ya Ramadhan, Swaum ya lonjezo lake ndi kukwaniritsa lonjezo lomwe lili lomvera Allah m'malo mwa iye.
Ndipo amene wamasula pa vuto lina lake ndipo vutolo nkutha mkatikati mwa usana wa mwezi wa Ramadhan, ndiye kuti adzafunika kusala komwe kwatsalako. Ndipo ngati kafiri walowa Chisilamu, kapena wayeretsedwa mzimayi amene anali kumwezi, kapena wodwala wachira, kapena wapaulendo wabwera ku ulendo wake, kapena mwana watha msinkhu, kapena wamisala wachira mkatikati mwa usana, pomwe iwo anali ololedwa kusamanga; ndiye kuti adzafunika kuchita Qadhwa, ngakhale kuti anamanga kotsala kwa tsikulo. Ndipo sizikuloledwa kwa amene walolezedwa kusamanga m'mwezi wa Ramadhan kuti amange Swaum ina iliyonse yosakhala ya Ramadhan m'mwezi wa Ramadhaniwo.

**SWAUM YA KUFUNA KWA MUNTHU:**

Ndipo yomwe ili yopambana kwambiri ndiye yakumanga tsiku, tsiku lina ndikudya, kenako Swaum ya lolemba ndi lachinayi, kenako kumanga masiku atatu mwezi uliwonse, ndipo mwa atatuwo omwe ali abwino kwambiri ndi masiku oyera omwe ndi pa (13, 14 ndi 15) m'mwezi ulionse wa chithunzi. Ndipo ndi Sunnat kumanga masiku ochuluka a mwezi wa Muharram ndi Shaabaan, pa (10) mwezi wa Muharram, pa (9) mwezi wa Dhulhijjah, ndi masiku asanu ndi limodzi a mwezi wa Shawwaal. Ndipo sibwino kusankha mwezi wa Rajab, tsiku lachisanu ndi loweluka pomanga, ndi kumanga tsiku lachikaiko lomwe ndi tsiku la pa (30) m'mwezi wa Shaabaan ngati kunali kopanda mitambo. Ndipo zili Haraam kumanga masiku a Eid ya Fitr, ndi Eid ya Adha, ndi pa (11, 12 ndi 13) m'mwezi wa Dhulhijjat, kupatula amene ali ndi mulandu wolipira chinyama cha Tamattu, kapena Qiraan ku Hajj.

**ZIDZIWITSO:**

- Munthu amene ali ndi hadath yaikulu monga amene ali ndi janaba, wamkazi amene ali kumwezi ndi amene ali ndi Nifaas, awiriwa akayeretsedwa Fajr isanatuluke, zikuloledwa kwa iwo kuchedwetsa kusamba mpaka nthawi ya

pambuyo pa Azaan ya Fajr, ndi kutsogoza kudya daku pa kusambako, ndipo Swaum idzakhala ili bwinobwino.

- Zikuloledwa kwa mayi kugwiritsa ntchito mankhwala kuti aichedwetse hidhwi yake (kuti isabwere msanga) m'mwezi wa Ramadhan ndi cholinga chofuna kuchitira limodzi ndi Asilamu ibaadat yawo, ngati sipangakhale vuto la mankhwalawo.
- Zikuloledwa kwa munthu womanga kumeza malovu, kapena makhololo akakhala kuti ali mkamwa.
- Mneneri (SAW) anati "*Um'mah wanga udzakhalabe pa mtendere akamafulumira kumasula ndi kuchedwetsa kudya daku*" **(Ahmad.)** Ananenanso (SAW) kuti "*Deen idzakhalabe yopambana anthu akadzakhala akufulumira kumasula, chifukwa Ayuda ndi Akhristu amachedwetsa kumasula*" **(Abu Dawood)**.
- Zili Sunnat kuchita Du'aa nthawi yomasula, Mtumiki (SAW) anati "*Ndithu munthu womanga ali ndi Du'aa yosabwezedwa pa nthawi ya kumasula kwake*" **(Ibn Majah)** ndipo ma Du'aa ena amene anadza pa nthawi yomasula ndi mau ake (SAW) onena kuti: "*Ludzu latha ndipo misempha yanyowa ndiponso malipiro atsimikizika Allah akalola*." **(Abu Dawood.)**
- Ndi Sunnat kuti kumasula kudzikhala ndi tende wamuwisi, ndipo ngati sanapeze ameneyo ndiye kuti amasulire tende ouma, ndipo ngati sanam'pezenso ameneyo ndiye kuti amasulire madzi.
- Munthu womanga ayenera kupewa kugwiritsa ntchito Kuhl (wanja) amene ali paudala wakuda yemwe amapakidwa m'maso, kudonthetsera zinthu za madzimadzi m'diso kapena mkhutu panthawi imene akusala, pofuna kuthawa kusiyana maganizo pa zimenezi, koma ngati zitafunika kutero monga mankhwala, ndiye kuti palibe vuto ngakhale kukoma kwa mankhwalawo kutafika kum'mero, ndipo Swaum yake ili bwino.
- Zili Sunnat kugwiritsa ntchito miswaki m'nthawi zonse za kumanga mopanda kuipa kulikonse zomwe zili zoona zake.
- Zili waajib kwa amene akumanga kusiya miseche, ukazitape, bodza ndi zina zotero. Ngati wina wake atafuna zosambulana naye kapena kutukwanana naye, ayenera kumuuza kuti "Ine ndili pa swaum". Ndipo chifukwa chosamalira lirime lake ndinso ziwalo zake zina ku machimo, ndiye kuti akusamalira swawmu yake, pakuti inadza Hadith kuchokera kwa Mtumiki (SAW), Iye anati: "*Amene sanasiye liwu labodza ndi kuligwiritsa ntchito, ndiye kuti kwa Allah palibe chifukwa choti angasiyire chakudya chake ndi chakumwa chake*". **(Bukhaari)**
- Ndi Sunnat kwa amene waitaniridwa chakudya ndipo ali ndi swaumu kuti am'pangire dua mwini chakudyacho, ndipo ngati anali wosamanga, adye.
- Usiku wa Lailatul Qadr ndi usiku wopambana m'chaka chonse. Ndipo kupezeka kwake kumakhala makamaka mu khumi lomaliza la mwezi wa Ramadhan, kwenikweni mu usiku wa pa (27). Ndipo ntchito yabwino yomwe ingagwiridwe mu usiku umeneu ndi yopambana kwambiri kuposa ntchito yabwino yomwe ingagwiridwe m'miyezi (1000). Ndipo kuonekera kwa Lailatul Qadr kuli ndi zizindikiro, zina mwa izo: Kutuluka dzuwa m'mawa mwake lili loyera lopanda nyenje zambiri, kuli bata. Ndipo Msilamu atha kukumana nayo iye asakudziwa, choncho chofunika kwa iye ndikulimbikira Ibaadat m'mwezi wa Ramadhan, kwenikweni mu khumi lomaliza.

Ndipo achitire khama kuti usamudutse usiku wina ulionse wopanda kuswalimo. Ndipo akafuna kuswali Taraweeh pa jamaat asachoke kufikira Imaam atamaliza kuswalitsa Taraweeh yonse kuti alembedwe kuti waswali usiku wonse.

- Amene waiyamba Swaum ya kufuna kwake zili Sunnat kwa iye kukwaniritsa koma sizili waajib, ngati ataiyipitsa mwadala palibe vuto ndiponso safunika kuibweza.

## • ITIKAAF

Kumeneku ndiko kudziumiriza kwa Msilamu wa nzeru zake kukhala mu Mzikiti chifukwa cha Ibaadat. Ndipo zikufunikira kuti wochita Itikafuyo akhale woyera ku Hadath yaikulu. Ndipo wochita Itikaf asatuluke mu Mzikiti pokhapokha pa chinthu chofunika kwa iye; monga kudya, kupita ku chimbudzi ndi kusamba kwa waajib, mwa chitsanzo. Ndipo Itikaf idzaonongeka chifukwa cha kutuluka mu Mzikiti popanda chifukwa chovomerezeka, komanso kugonana. Ndipo zili Sunnat kuchita Itikaf nthawi ina iliyonse, koma m'mwezi wa Ramadhan ndiye chizimu, kwenikweninso khumi lomaliza. Ndipo kuchepa kwa nthawi ya Itikaf ndi kamphindi kochepa, ndipo ndibwino kuti nthawiyo isachepere pa usana ndi usiku. Ndipo mkazi asachite Itikaf pokhapokha ndi chilolezo cha mwamuna wake. Ndipo zili Sunnat kwa amene akuchita Itikaf kuti atanganidwe ndi Ibaadat komanso ntchito zabwino, achepetse kuchita zinthu zololedwa kuzichita, ndiponso apewe zinthu zimene sizikumukhudza.

# HAJJ NDI UMRAT

**Hajj ndi Umrat imakhala waajib kamodzi pa moyo wonse. Ndipo zofunikira zake kuti zikhale waajib ndi izi: (1)** Munthuyo akhale Msilamu **(2)** Wanzeru zake (osati wamisala) **(3)** Wotha msinkhu **(4)** Akhale mfulu **(5)** Pakhale kuthekera komwe ndi kupeza kamba wa pa ulendo ndi chokwera.

Ndipo amene anasiya dala kuchita Hajj mpaka kumwalira, aperekedwera chuma kuchokera m'chuma chake chomwe wasiya ndikukam'chitira Hajj ndi Umrat. Ndipo Hajj siingatheke kwa munthu Kafiri ndi wamisala, koma itha kutheka kwa mwana ndi kapolo (koma kuti) siingakwanire kwa awiriwo kukhala Hajj ya chilamulo cha Chisilamu. Ndipo amene sangathe kukachita Hajj monga wosauka akakongola ndalama ndi kukachita Hajj, ndiye kuti Hajj yakeyo yatheka. Ndipo amene wachita Hajj ya wina wake kumachita kuti iye mwini sanadzichitire Hajj ya chilamulo cha Chisilamu; Hajj imeneyo idzakhala Fardh kwa iye mwiniyo.

**IHRAAMU:** Zili Sunnat kwa amene akufuna kuchita Ihramu kuti asambe, adzikonze, adzinunkhiritse, avule chovala chosokedwa ndipo avale chilundu ndi nsalu yofunda, ziwirizi zikhale zoyera zaukhondo, kenako anene kuti LABBAYKALLAHUMMA UMRATAN, kapena kuti HAJJAN kapena kuti HAJJAN WA UMRATAN. Ngati ataopa china chake adzafunikira anene kuti: Koma ngati chitandilepheretsa china chake ndiye kuti ndidzamasulira pamene ndalepheretsedwapo.

Ndipo wofuna kuchita Hajj ali ndi kusankha pakati pa machitidwe atatu a kachitidwe ka Ibaadat: Tamattu, Ifrad ndi Qiran, ndipo mwa kachitidwe konseka komwe kali kabwino kwambiri ndi ka Tamattu: Tamattu ndiko kuchita Niyyat ya Umrat m'miyezi ya Hajj ndi kumaliza kuchita Umratyo, kenako nkudzachita Niyyat ya Hajj m'chaka chomwecho. Ndipo Ifrad ndiko kuchita Niyyat ya Hajj payokha. Pomwe Qiran ndiko kuchita Niyyat ya zinthu ziwirizi, kapena kuchita Niyyat ya Umrat, kenako n'kuilowetsa Hajj mu Umratmo asanayambe kuchita Twawaaf.

Choncho amene wafuna kuchita Hajj akakhazikika pa chokwera chake adzanena Talbiyat ponena kuti: LABBAIKAL LAHUMMA LABBAIKA, LABBAIKA LAA SHARIKA LAKA LABBAIKA, INNAL HAMDA WANNI'MATA LAKA WAL MULK, LAA SHARIKA LAKA.[1] Ndipo ndibwino kuchulutsa kunena Talbiyat ndi kukweza mau ponena Talbiyat kupatula akazi.

**ZOLETSEDWA PAMENE MUNTHU ALI M'MAPEMPHERO A HAJJ NDI UMRAT**

**Zilipo zisanu ndi zinayi: 1)** Kumeta tsitsi. **2)** Kuwenga zikhadabo. **3)** Kuvala chosokedwa, pokhapokha ngati sanapeze chilundu, ndiye kuti adzavala mtocha, kapena sanapeze patapata,ndiye kuti adzavala ma Khuf, ndipo awadule kufikira atakhala pansi pa misomali. **4)** Kuvindikira mutu kwa munthu wa mwamuna. **5)** Kugwiritsa ntchito mafuta onunkhira pa thupi pake ndi pa nsalu zake. **6)** Kupha nyama ya m'tchire yomwe ili yololedwa. **7)** Kumangitsa ukwati; kutero ndi haraam, koma palibe kulipira. **8)** Kugwirana mwakhumbo logonana kosakhala kumaliseche, ndipo kulipira kwake ndi mbuzi, kapena kumanga masiku atatu, kapena kuwadyetsa masikini asanu ndi mmodzi. **9)** Kugonana ndi mkazi: Choncho ngati kunali asanamasule kumasula koyamba; ndiye kuti Hajj yake yaonongeka,

[1] (Oh, Mbuye wanga ndilipo ine ndilipo, ndilipo ine, Inu mulibe wothandizana naye ndithu ine ndilipo, ndithu matamando onse, mtendere onse ndi ufumu ndi zanu, Mulibe wothandizana naye).

koma padzafunika kuti akwaniritse Hajjiyo ndi kudzachita Qadhwa chaka chinacho, ndi kuzinganso ngamira yomwe idzagawidwe kwa anthu osauka a m'Makkat. Ndipo ngati kugonanako kunachitika pambuyo pa kumasula koyamba, ndiye kuti Hajj yake siinaonongeke koma zidzakhala waajib kwa iye kuzinga ngamira.
Ndipo ngati kutapezeka kugonana pa nthawi ya Umrat, kugonanako kudzaononga Umratyo, ndipo adzalipira mbuzi, koma adzafunika kuchita Qadhwa. Hajj kapena Umrat palibe chomwe chingaononge ziwirizi kupatula kugonana. Ndipo pa zinthu zoletsedwazi wamkazi ali ngati wamwamuna, kungoti wamkaziyo akuloledwa kuvala chosokedwa, koma asavindikire nkhope yake, ndiponso asavale magolovesi.
**KULIPIRA KULI PAWIRI: (1) Munthu ali ndi kusankha:** Komwe ndi kulipira kwa chifukwa chometa tsitsi, kapena kudzinunkhiritsa, kapena kuwenga zikhadabo, kapena kuvindikira mutu, kapenanso kuvala chosokedwa kwa anthu amuna. Choncho ali ndi kusankha pakati pa kumanga masiku atatu, kapena kuwadyetsa masikini asanu ndi mmodzi. Ndipo masikini aliyense apatsidwe chakudya chokwanira theka la Swaa, chomwe ndi cholemera (1½kg), kapena azinge mbuzi. Ndipo kulipira kwa chinyama cha m'tchire adzapereka cholingana ndi chimene chaphedwa kuchokera mu zifuyo ngati chilipo chofanana nacho, koma ngati palibe chofanana nacho adzapereka ndalama zolingana ndi mtengo wake.
**(2) Kulipira mwa ndondomeko:** Komwe ndi kulipira chifukwa cha munthu wa Tamattu ndi wochita Qiran,dipo lake ndi mbuzi, ndipo dipo la kugonana, ndi kuzinga ngamira, choncho ngati sanapeze zinyamazi, ndiye kuti adzamanga masiku atatu ku Hajj, ndikukamanganso masiku asanu ndi awiri akadzabwelera kwawo. Ndipo chinyama cholipidwa kapena kudyetsa chakudya zisakhale zowapatsa ena koma anthu osowa a mu Haraam.
**KULOWA KWA MUMZINDA WA MAKKAT**: Wochita Hajj akalowa mu mzikiti wa haraam adzanena Du'aa yomwe inaikidwa kunena m'mizikiti ina yonse, kenako adzayamba ndi Twawaaf ya Umrat ngati ali wochita Tamattu, kapena kuyamba ndi TWAWAAF Qudoom ya munthu amene wangofika kumene ngati ali wa Ifrad kapena wa Qiràn. Ndipo adzafunda nsalu yake moika katikati ya nsaluyo kunsi kwa phewa lake lamanja, ndipo nsonga zake ziwiri za nsaluyo adzaika pa phewa lake lakumanzere. Ndipo poyamba Twawaaf adzayambira pamene pali mwala wakuda ndipo adzaugwira ndi kuupsopsona kapena kuuloza ndipo adzanene kuti: Bismillahi wAllahu akbar: adzachita zimenezi mu kuzungulira kulikonse. Kenako adzaiyika Kaabat chakumanzere kwake nazungulira kasanu ndi kawiri, ndipo adzayenda ndawala mu kuzungulira kutatu koyambirira m'mene angathere, ndi kudzayenda m'kuzungulira kunayi. Ndipo mu nthawi iliyonse imene angayang'anizane ndi kona ya Yamaani adzakhudza ngati angathe, ndipo adzanena pakati pa makona awiri a Kaabat kuti: "Rabbanaa aatinaa fid-dunyaa hasanatan wa fil-aakhirati hasasanan waqinaa adhaaban-naari - Oh! Mbuye wathu, tipatseni pano pa dziko lino lapansi zabwino komanso pa Tsiku Lomaliza zabwinonso komanso mukatiteteze ku chlango cha moto" Ndipo adzapempha m'kuzungulira kwina kulikonse Duaa imene angafune. Kenako akamaliza kuchita Twawaaf adzaswali marakaat awiri kumbuyo kwa Maqam Ibrahim ngati zingatheke.Adzawerenga m'marakaat awiriwo surat ziwiri Kafiroon ndi Ikhlas, kenako akadzamaliza adzapita

kukamwa madzi a Zamzam ndipo adzachulutse kumwa madziwo nabweleranso ku mwala wakuda uja ndikuukhudza ngati kungatheke. Kenako adzachita Duaa pakati pa mwala wakuda ndi khomo, akadzamaliza Duaa adzapita ku Swafa ndikukakwera pa phiripo nadzanena kuti: "Ndikuyambira kumene Allah anayambira", nadzawerenga mau a Allah onena kuti: (***Ndithudi Swafa ndi Marwat ndi zizindikiro zolemekezera chipembedzo cha Allah. Choncho amene akukachita mapemphero a Hajj kunyumbayo, kapena kukachita Umrat, sikulakwa kwa iye kuzungulira pamenepo pakati pa mapiri awiriwo. Ndipo amene achite chabwino modzipereka adzalipidwa. Ndithudi Allah Ngothokoza Ngodziwa***). **(Surat 2: 158.)** Ndipo adzanena Takbir ndi Tahlil, ndipo adzayang'ana molunjika ku Kaabat nanyamula manja ake ndikuchita Duaa. Kenako adzatsike nayenda mpaka pa chizindikiro chobiriwira cha green, kenako adzayenda ndawala mpaka pa chizindikiro china nayenda mpaka akafike pa Marwat, ndipo adzachita zomwe anachita pa Swafa kupatula kuwerenga Ayat. Kenako adzatsika nkukachita monga zomwe anachita mu kuyenda koyamba mpaka adzakwanitse kuyenda kusanu ndi kuwiri. Kuchokera ku Swafa kupita ku Marwat kuyenda kumodzi, ndipo kuchokera ku Marwat kupita ku Swafa kuyendanso kumodzi, ndipo choncho mpaka kasanu ndi kawiri. Ndipo akamaliza adzayepula tsitsi lake kapena kumeta, ndipo kumeta ndibwino kwambiri kupatula pa Umrat ya amene akuchita Tamattu chifukwa choti iye pambuyo pake adzachita Hajj. Tsopano munthu wochita Qiran ndi wa Ifrad sangamasule pambuyo pa TWAWAAF Qudoom mpaka atagenda chipilala cha Aqabat tsiku la Eid, ndipo malamulo amenewa wamkazi ali ngati wamwamuna, kungoti wamkaziyo sadzayenda ndawala pa TWAWAAF ndi pa Sa'ay apa ndi pakati pa Swafa ndi Marwat.

**KACHITIDWE KA HAJJ**: Ndipo likakwana tsiku la Tarwiyat (8 Dhul hijjat) adzachita Niyyat ya Hajj ngati amachokera m'nyumba yake yomwe ili m'Makkat ndipo adzapita ku Mina kuti akagone kumeneko usiku wa (9). Choncho dzuwa likadzatuluka m'mawa wa pa (9) Dhul hijjat adzayenda ulendo wopita ku Arafat, ndipo likapendekeka dzuwa adzaswali Zuhr ndi Asr mophatikiza komanso mopungula marakaat. Ndipo Arafat yonse ndi malo woti munthu atha kuima kupatula chigwa cha Uranat, ndipo adzachulutsa kunena mau oti: LA ILAHA ILL ALLAHU WAH, DAHU LAA SHARIKA LAHU, LAHUL MULKU WALAHUL HAMDU WAHUWA ALAA KULLI SHAI – IN QADEER. Ndipo adzalimbikira kuchita Duaa ndi Toba ndi kufunitsitsa mtendere kwa Allah. Ndipo dzuwa likalowa adzanyamuka ulendo wa ku Muzdalifat modekha komanso modzilemekeza akunena Talbiyat momukumbukira Allah. Ndipo akakafika ku Muzdalifat akaswali pamenepo Swalaat ya Maghrib ndi Isha mophatikiza mopungula marakaat nagona pamenepo. Kenako m'mawa adzaswali Fajr mu nthawi yake yoyambirira, ndipo adzakhala ali pamenepo akuchita Duaa mpaka kutaonekera kucha, kenako adzanyamuka dzuwa lisanatuluke. Ndipo akafika pa chigwa cha Muhassir afulumire kwambiri poyenda ngati angathe mpaka adzafike ku Mina ndikuyamba kuchigenda chipilala cha Aqabat, ndipo adzachigenda ndi timiyala tisanu ndi tiwiri tating'onoting'ono, ndipo pogenda kamwala kalikonse adzanena Takbir. Ndipo adzanyamula dzanja lake pogenda, ndipo padzafunikira kuti kamwalako kadzagwere m'dzenje ngakhale sikadamenye chipirala chenichenicho. Ndipo akangoyamba kugenda adzalekeza

kunena Talbiyat, kenako adzazinga nyama yake, ndipo kenako adzameta mutu wake kapena kuuyepula, koma kumeta ndibwino kwambiri. Ndipo ndikuponya kumeneko chilichonse chidzakhala Halal kwa iye kupatula kugona ndi mkazi, ndipo kumeneko ndiye kumasuka kwa Hajj koyamba. Kenako adzapita ku Makkat nakachita Twawaaf Ifadhwa (yochita pochokera ku Mina). Imeneyo ndi Twawaaf yomwe ili waajib, Hajj imakwanira chifukwa cha Twawaaf imeneyo. Kenako adzayenda ndawala pakati pa Swafa ndi Marwat ngati amachita Tamattu, kapena ngati sanayende ndawala pa Twawaaf ya Qudoom, choncho akachita zimenezo ndiye kuti chilichonse chidzakhala Halaal kwa iye komanso akazi.

Kumeneko ndiye kumasuka (kwa Hajj) kwachiwiri. Kenako adzabwereranso ku Mina nakagona usiku wake kumeneko, kutero ndi waajib, ndipo ali ku Minako adzagenda zipirala pambuyo popendekeka dzuwa m'masiku amenewo, chipirala chilichonse adzachigenda ndi timiyala tisanu ndi tiwiri, adzayambira kugenda chipirala choyambirira ndi timiyala tisanu ndi tiwiri, kenako adzapita patsogolo naima ndikum'pempha Allah, kenako n'kupita ku chipirala cha pakati nachonso adzachigenda chimodzimodzi ndipo pambuyo pake adzachita Du'aa, kenako adzagenda chipirala chomaliza chomwe ndi cha Aqabat ndipo asaime pamenepo. Kenako mu tsiku lachiwiri adzagenda chimodzimodzi, ndipo ngati atafuna kuti afulumire adzachoka dzuwa lisanalowe, ndipo ngati dzuwa litalowa pa (12) Dhul hijjat iye ali pa Mina adzakakamizidwa kuti agone pa Minapo ndikugenda zipilala m'mawa mwake, pokhapokha ngati chigulu cha anthu chitam'tsekereza iye atatsimikiza za kunyamuka, ndiye kuti palibe vuto kunyamuka ngakhale dzuwa litalowa. Ndipo wochita Qiràn malamulo ake ali chimodzimodzi ngati a wochita Ifrad, kungoti iye akufunika kuzinga nyama ngati wochita Tamattu. Ndipo akafuna kunyamuka ulendo kupita kwao sadzanyamuka mpaka atadzailawira Kaabat pochita Twawaaf, kuti Kaabatyo idzakhale mapeto a chipangano chake kupatula amene ali ndi hidhwi ndi amene ali ndi Nifaas, pakuti kwa awiriwa Twawaaf ya malawirano idzakhululukidwa. Choncho ngati atatanganidwa pambuyo pake ndi malonda adzabwerezanso Twawaaf ya malawirano. Ndipo amene adzabwerera ngati anali pafupi wanyamuka asanalawire,abwera ngati ali pafupi, koma ngati anali patali sadzabwerera koma adzafunika kulipira nyama.

## NSICHI ZA HAJJ

**Nsichi za Hajj zilipo zinayi:- 1)** Kuchita Ihram: Komwe ndi Niyyat yolowera m'mapemphero a Hajj. **2)** Kuimilira pa Arafat (Ifaadhwa). **3)** Twawaaf ya ziyarat (yomwe imachitika pochokera ku Mina). **4)** Ndawala ya Hajj.

**Zofunika zake zilipo zisanu ndi ziwiri**: **1)** Kuchita Niyyat kuchokera pa Meeqaat. **2)** Kuimirira pa Arafaat mpaka usiku. **3)** Kugona pa Muzdalifat mpaka pambuyo pa theka la usiku. **4)** Kugona pa Mina mausiku a masiku a Tashreeq (pa 11, 12, ndi 13 Dhul hijjat). **5)** Kugenda zipilala. **6)** Kumeta tsitsi kapena kuyepula. **7)** Twawaaf ya malawirano. **8)** Kuzinga chinyama kwa amene wachita tamattu'u kapena qiran.

**Nsichi za Umrat zilipo zitatu**:

**1)** Kuchita Ihram. **2)** Twawaaf ya Umrat. **3)** Ndawala ya Umrat.

## ZOFUNIKA ZAKE ZILIPO ZIWIRI

**1)** Kuchita Ihram kuchokera pa Meeqaat. **2)** Kumeta tsitsi kapena kuyepula.

**Amene wasiya nsichi imodzi:** Ibaadat ya Hajj siingakwanire pokhapokha ndi nsichi imeneyo, ndipo amene wasiya chinthu cha waajib Chidzasokedwa ndi kulipira nyama, ndipo amene wasiya Sunnat palibe vuto kwa iye.

**ZOFUNIKIRA KUTI TWAWAAF YA KAABAT ITHEKE**

**Zilipo khumi ndi zitatu: 1)** Munthuyo akhale Msilamu. **2)** Wanzeru zake osati wamisala. **3)** Achite Niyyat yakeyake. **4)** Kukwanira nthawi yochitira Twawaaf. **5)** Kubisa umaliseche kwa amene angathe. **6)** Kudziyeretsa ku hadath osati ya mwana wakhanda. **7)** Kukwanitsa kuzungulira kasanu ndi kawiri motsimikiza. **8)** Kuiyika Kaabat cha kumanzere kwake, ndipo kuzungulira komwe alakwitse posaiyika Kaabatyo kumanzere kwake adzakubwerezanso. **9)**Asabwerere pa kuyenda kwake. **10)**Kuyenda kwa amene angathe. **11)** Kuwirikiza pakati pa kuzunguliRako. **12)**Kuchitike mkati mwa mzikiti wa Makkat. **13)**Twawaaf iyambire pa mwala wakuda.

**SUNNAT ZA TWAWAAF**: Kuukhudza mwala wakuda ndi kuupsopsona, kunena Takbir pafupi ndi mwalawo, kukhudza kona ya Yamaani, kuonetsera phewa limodzi, kuyenda mwa ndawala ndi kuyenda m'malo ake ndipo ofunika kutero, kuchita Duaa ndi Zikr mkatikati mwa Twawaaf, kuiyandikira Kaabat, ndi kuswali marakaat awiri pambuyo pake cha kumbuyo kwa Maqaam Ibrahim.

**ZOFUNIKIRA ZA NDAWALA ZILIPO ZISANU NDI ZINAYI**: **1.**Munthuyo akhale Msilamu. **2.** Wa nzeru zake. **3.** Kuchita Niyyat. **4.** Kuwirikiza. **5.**Kuyenda kwa amene angathe.**6.**Kukwaniritsa kasanu ndi kawiri. **7.** Kukwaniritsa kuchita ndawala pa malo a pakati pa Swafa ndi Marwat. **8.** Ichitike pambuyo pa Twawaaf yolondola. **9.** Koyambirira kakhale kuchokera ku Swafa ndipo kachiwiri ku Marwat.

**SUNNAT ZA PA NDAWALA**: Kudziyeretsa ku hadath ndi nyansi, kubisa maliseche, kuchita Zikr ndi Duaa mkatikati mwake, kuthamanga ndi kuyenda pa malo ake, ndi kukwera pamwamba pa mapiri awiri omwe ndi Swafa ndi Mearwat, ndi kuwirikiza pakati pa ndawala ndi Twawaaf.

**CHIDZIWITSO:** Ndibwino kwambiri kugenda zipilala tsiku lomwelo, ndipo ngati wachedwetsa kugenda kwa tsiku lina lake kuti adzagenda mawa, kapena wakuchedwetsa kugenda konse kuti adzagende kumapeto kwa masiku a Tashreeq n'zotheka.

**QURBAAN:** Iyi ndi Sunnat ya mphamvu, ndipo likalowa khumi la mwezi wa Dhul hijjat zili haraam kwa amene akufuna kuti adzazinge chinyama kudula kalikonse mu tsitsi lake, kapena zikhadabo zake, kapena khungu lake kufikira atazinga nyama yake.

**AQEEQAT**: Imeneyo ndi Sunnat pomuzingira mwana wamwamuna mbuzi ziwiri, ndipo wamkazi imodzi, izingidwe tsiku la chisanu ndi chiwiri kuchokera tsiku limene anabadwa. Ndipo zili Sunnat mu tsiku la chisanu ndi chiwiri kumeta mutu wa mwana wa mwamuna, ndi kupereka sadaka siliva wolemera ngati tsitsilo, ndipo pa tsiku limeneli apatsidwe dzina, ndipo mwa maina abwino ndi Abdullah komanso Abdul Rahmaan. Ndipo ndi Haraam kum'patsa dzina kuti kapolo wa chosakhala Allah; monga Abdun-nabiyy ndi AbdulRasul. Ngati itagwirizana nthawi ya Aqeeqat ndi Qurbaan ndiye kuti kutheka kwa chimodzi mwa ziwirizi kudzapangitsa kutheka chinacho.

**PHINDU:** Munthu amene walowa mu Mzikiti wa Mtumiki (SAW) ayambe ndi rakaat ziwiri za Tahiyyatul Masjid. Kenako afike pa manda wolemekezeka

ndikuima molunjika nkhope ya Mtumiki (SAW) msana wake uli ku Qiblat. Mu mtima mwake mudzaze kulemekeza ngati akumuona (SAW) n'kuchita salaam monena kuti: "Assalaam alayka yaa Rasuula Allah" ataonjezera pamauwa ndibwino. Kenako asunthire ku manja mulingo wotambasula dzanja limodzi ndipo anene : "Assalaam alayka yaa Abaa Bakr, Assalaam alayka yaa Omar Al Faarooq, Allaahumma ajizhumaa an nabiyyihimaa wa anil Islaam khairan." Kenako ayang'ane ku Qiblat- Hujrat ili kumanzere kwake nachita duwa.

## ICHI NDI CHIDULE CHA NTCHITO ZA HAJJ MWA NDONDOMEKO:

| IBAADAT YA HAJJ | TAMATTU | QIRAN | IFRAD |
|---|---|---|---|
| KUYAMBA NDI IHRAAM KOMANSO TALBIYAH | NDIKUNENA TALBIYAH YA UMRAT NDIKUCHITA TAMATTU NDI UMRATYO NDIKUKACHITANSO HAJJ | NDIKUNENA TALBIYAH YA UMRAT KOMANSO HAJJ | NDIKUNENA TALBIYAH YA HAJJ |
| KENAKO | TWAWAAF YA UMRAT | TWAWAAF YA POFIKA | TWAWAAF YA POFIKA |
| KENAKO | NDAWALA YA UMRAT | NDAWALA YA HAJJ | NDAWALA YA HAJJ |
| KENAKO | KUYEPULA TSITSI (KUMALIZITSA IBAADAT KOKWANIRA) | AKHALE ALI MU IHRAM YAKE | AKHALE ALI MU IHRAM YAKE |
| TSIKU LA 8 ASANA SWALI ZUHR | ACHITE NIYYAT YA HAJJ KUCHOKERA MMAKKAT KENAKO APITE KU MINA | KUPITA KU MINA | KUPITA KU MINA |
| TSIKU LA 9 LITATULU KA DZUWA | APITE KU ARAFAT NDIPO AKASWALI ZUHR NDI ASR MOPHATIKIZA KOSWALIRATU ASR KOMANSO MOPUNGULA MARAKAAT KENAKO AZINGOCHITA MA DUA MPAKA KULOWA KWA DZUWA | | |
| PAMBUYO POTULUKA DZUWA | ANYAMUKE KUPITA KU MUZDALIFAH NDIPO AKAKAFIKA AKASWALI MAGHRIB NDI ISHA NDIKUKAGONA PAMENEPO MPAKA THEKA LA USIKU NDIPO ZILI SUNNA KUTERO CHIFUKWA CHA KUTALIKIRA KWA FAJR | | |
| PAMBUYO PA TSIKU LA EID POLOWA PAMBUYO PA FAJR DZUWA LISANATULUKE | KUPITA KU MINA NDI KUKAGENDA CHIPILALA CHA AQABAH | | |
| | KUZINGA NYAMA | KUZINGANYAMA | ======= |
| | KUMETA KAPENA KUYEPULA TSITSI KENAKO ACHITE TWAWAAF YA POCHOKERA KU MINA. NDIPO KUMASULA KOYAMBA KUDZAKWANIRA POCHITA ZINTHU ZIWIRI MWA ZITATUZI, NDIPO KUMASULA KWA CHIWIRI KUDZAKWANIRA POCHITA ZINTHU ZITATU | | |
| | NDAWALA YA HAJJ | ======== | ========= |
| MASIKU A PA 11, 12 NDI 13 KWA AMENE WACHEDWA | KUGENDA ZIPILALA AGENDE CHIPILALA CHACHING'ONO KENAKO CHIPILALA CHAPAKATI KENAKO CHIPILALA CHACHIKULU PAMBUYO PA KUPENDEKA KWA DZUWA | | |
| ALI PAFUPI KUNYAMUKA KUPITA KWAWO | ACHITE TWAWAAF YA MALAWIRANO, NDIPO IMAKHULULUKIDWA KWA AMENE ALI NDI HIDHWI NDI NIFAAS | | |

# MAPHINDU OSIYANASIYANA

✸ **TCHIMO: Limafufutidwa ndi kukhululukidwa ndi zinthu zina mwa izi:-** Kulapa koona, kupempha chikhululuko, ntchito zabwino, kuyesedwa ndi mavuto, sadaka, Duaa ya munthu wina, choncho ngati litatsala tchimo lina lake ndipo Allah sanamukhululukire iye adzalangidwa m'manda chifukwa cha tchimo limenelo kapena pa tsiku la Kiyaamat, kapena m'moto wa Jahannam kufikira atayeretsedwa ku tchimolo, kenako adzalowa ku Jannat ngati anamwalira ndi Tauheed (akukhulupirira umodzi wa Allah). Ndipo ngati atamwalira ali pa ukafiri, kapena akuchita shirk, kapena akuchita uchiphamaso akasungidwa m'moto wa Jahannam mpaka kalekale.

Zinthu zoipa ndi machimo zili ndi zotsatira pa munthu. Ndipo zotsatira zake mu mtima wa munthu ndi zoipa ndi machimowo zimayambitsa kusungulumwa ndi mdima, kunyozeka, matenda ndipo zimatsekereza mtimawo kumumvera Allah.

**Pa chipembedzo:** Zimayambitsa monga zanenedwazi ndiponso zimamanitsa ntchito yabwino, Duaa ya Mtumiki (SAW), ya angero ndi ya anthu okhulupirira. **Ndipo pa riziki:** zimamanitsa riziki, zimachotsa mtendere komanso zimachotsa madalitso a chuma. **Ndipo pa munthu:** Zimachotsa madalitso a moyo wa munthu, zimayambitsa umoyo wovutika komanso kuvuta kwa zinthu. **Ndiponso pa ntchito zosiyanasiyana:** zimalepheretsa kulandiridwa ntchitozo. **Ndiponso ku gulu:** Zimachotsa mtendere wa chitetezo, zimayambitsa kukwera mitengo ya zinthu, kupatsidwa atsogoleri opondereza komanso adani, kutsekerezedwa mvula ndi zina zotero.

✸ **MAGANIZO NDI MADANDAULO:** Mtendere wa mu mtima ndi kusangalala kwake komanso kuchoka kwa maganizo ndi madandaulo ake ndicho chofuna cha aliyense, ndipo umoyo wabwino umapezeka ndi kutero, ndipo kuti zipezeke zimenezo pali njira za chipembedzo, chilengedwe ndi ntchito, sizingasonkhane pokhapokha kwa okhulupirira.

**Ndipo zina mwa izo ndi izi:- 1.** Kukhulupirira mwa Allah. **2.** Kuchita zolamulidwa ndi kupewa zoletsedwa. **3**. Kuchita zabwino ku zolengedwa kudzera m'mau, machitidwe ndi mitundu ina ya zabwino. **4.** Kutanganidwa ndi ntchito zosiyanasiyana kapena maphunziro aphindu a uzimu kapena a dziko lapansi. **5.** Kusalingalira ntchito za mtsogolo kapena za m'mbuyo, koma atanganidwe ndi ntchito zake za tsiku ndi tsiku. **6.** Kuchulutsa kumukumbukira Allah. **7.** Kukamba za mtendere wa Allah oonekera ndi osaonekera. **8.** Kumuyang'ana amene wachepekedwa kuposa ife, ndi kusamuyang'ana amene wapatsidwa mtendere ochuluka kuposa ife pa zinthu za dziko lapansi. **9.** Kuyesetsa kuchotsa zifukwa zomwe zimayambitsa maganizo ndi madandaulo ndikupeza zifukwa zomwe zimayambitsa chisangalalo. **10.** Kuthawira kwa Allah ndi zina zomwe anali kudzithandizira nazo Mneneri (SAW), monga kuchita Duaa pofuna kuthetsa kuganiza ndi kudandaulo.

**PHINDU:** Ibrahim Khawwas (RA) ananena kuti "Zinthu zisanu ndi mankhwala a mtima: Kuwerenga Quràn molingalira, Kukhala ndi njala, Kuswali usiku, Kukhuzumuka ndi ma Du'aa kum'bandakucha ndi kukhalirana ndi anthu abwino.

Amene lampeza vuto ndipo wafuna kulichepetsa mphamvu ndi kulipeputsa alione kuti ndi lalikulu ndipo aganize kuti lili ndi sawabu zake, komanso aganize za kubwera vuto lalikulu kuposa ilo.

✷ **UKWATI**: Ndi Sunnat kukwatira kwa amene ali ndi chilakolako koma sakuopa kugwa m'chiwerewere, ndipo ukwatiwo ukuloledwa kwa amene alibe chilakolako, ndipo ndi waajib kwa amene akuopa kugwa m'chiwerewere, ndipo ukwati udzatsogozedwa pa Hajj ya waajib. Ndipo zili Haraam kumuyang'ana wamkazi.

**ZOFUNIKIRA ZA UKWATI**: **(1).** Kulozedwa awiri okwatiranawo: choncho nzosatheka kuyankhula kwa m'yang'aniri konena kuti: "Ndakukwatitsa mmodzi mwa atsikana anga" kumachita iye ali ndi atsikana ochuluka kuposera mmodzi. **(2).** Mwamuna wotha msinkhu, wochangamuka akondweretsedwe, nayenso mkazi amene ali mfulu, wanzeru zake akondweretsedwe. **(3).** Apezeke m'yang'aniri: Choncho n'kosatheka mkazi kudzikwatitsa yekha, komanso asamkwatitse amene sali m'yang'aniri wake, pokhapokha ngati atakana kum'kwatitsa ndi wolingana ndi kuyenerera naye. Ndipo amene ali woyenera kwambiri kum'kwatitsa mwana wamkazi ndiye Bambo, kenako Bambo a Bambo ake -omwe ndi agogo ngakhale mtundu wawo utapita patsogolo, kenako mwana wake wamwamuna wamkaziyo, kenako mwana wa mwana wake- mdzukulu, ngakhale mtundu wake utatsika, kenako achimwene a mimba imodzi, kenako achimwene ake mwa abambo, kenako mwana wa achimwene mpaka kumapeto. **(4).** Papezeke mboni: Choncho payenera kupezeka mboni ziwiri zachimuna zotha msinkhu, za nzeru zake, zachilungamo. **(5).** Mwa awiri okwatiranawa musapezeke zoletsa; monga kuyamwa bere limodzi, kapena chibale, kapenanso chipongozi.

✷ **AMENE ALI HARAAM KUWAKWATIRA**:

**A) Oyamba:** omwe ali haraam mpaka kalekale; Ndipo iwo ali mzigawo izi:

**(1).** Chifukwa cha chibale : omwe ndi amayi, agogo akazi ngakhale mtundu wawo utakwera, mwana wamkazi ndi mwana wamkazi wa mwana wam'muna ngakhale mtundu utatsika, chemwali aliyense, mwana wamkazi wa chemwali komanso mwana wamkazi wa mwana wake wam'muna, kapena mwana wake wamkazi, mwana wamkazi wa achimwene aliyense, ndi ana awo akazi komanso ana akazi a ana awo amuna ndi ana awo akazi ngakhale atatsika, azakhali komanso akulu awo kapena ang'ono awo a amayi ngakhale mtundu wawo utakwera. **(2).** Chifukwa cha kuyamwa bere limodzi : ndipo uharaam wake uli ngati wachibale mpaka pa chipongozi. **(3).** Chifukwa cha chipongozi: womwe ndi amayi a mkazi wake komanso agogo ake, aakazi a nthambi ziwiri za mtundu wake, ana aakazi owapeza ngakhale atatsika.

**B) Achiwiri:** omwe nkoletsedwa kuwakwatira pa nyengo ina ali mitundu iwiri:

**1)** Chifukwa cha kuphatikiza (mitala), monga kuwaphatikiza akazi awiri apachibale.

**2)** Chifukwa cha chifukwa chimene chingathe kuchoka, monga mkazi wa munthu wina.

**PHINDU:** Sizikuloledwa kwa makolo a munthu kum'kakamiza iye kuti akwatire amene sakumufuna, ndipo sizili waajib kuti awamvere makolowo pa zimenezo, ndipo pakutero sangakhale wonyoza makolo.

✷ **KUSIYA UKWATI**: Zili Haraam kumusiya mkazi pamene ali pa hidhwi, kapena Nifaas, kapena pamene ali woyera atagona naye koma ukwatiwo udzathabe. Ndipo sibwino kuthetsa ukwati popanda chifukwa koma ndi zololedwa ngati pali chifukwa, ndipo ndi sunnat kusiya ukwati kwa amene akupeza vuto ndi ukwati. Ndipo sizili waajib kuwamvera makolo awiri za kuthetsa ukwati. Ndipo amene

akufuna kuleka mkazi wake zili haraam kwa iye kumuleka kopitirira kamodzi (kamodzi n'kamodzi). Ndipo ndi waajib kumuleka pa nthawi yoti alibwino (sakusamba) ndipo sanagonane naye, choncho adzamuleka kamodzi namusiya mosaonjezera kumusiya kwina kosanjikiza apa mpaka kutatha kuyembekeza kwake, ndipo zili haraam kwa amene cha mbeta chake chili cha chibwerero kuchokera m'nyumba mwa mkaziyo, kapena mwamuna kum'tulutsa mkaziyo chisanakwanire chiyembekezo chake. Ndipo ukwati ungathe poyankhula (ponena kuti ndakusiya ukwati), choncho siungathe chifukwa cha niyyat yokha.

✸ **MALUMBIRO**: Kulipira chifukwa cha kulumbira kudzafunika ngati patapezeka zofunikira zinayi izi:-**1)** Kutsimikiza kulumbira: Choncho sikungachitike komanso (sikungatheke) ngati atalumbira ndi lirime lake mopanda kutsimikiza kulumbira ndipo kumeneko kumatchedwa kuti kulumbira kopanda pake, monga kunena kuti "ayi ndithu ndikulumbira Allah", ndikulumbira koti "E, ndi kulumbira Allah" poyamba kuyankhula. **2)** Kulumbirako kukhale pa chinthu cha mtsogolo choti chitha kutheka: Choncho kulumbirako sikungatheke pa chinthu choti chinachitika kale mosadziwa, kapena kudziganizira kuti akunena zoona, kapena mwa bodza akudziwa kumeneko ndikulumbira kogwa nako m'mavuto, komanso kuli m'gulu la machimo aakuluakulu, kapena walumbira chinthu chapatsogolo akudziganizira kuti akunena zoona n'kudzapezeka kuti sizili choncho. **3)** Wolumbirayo akhale kuti akulumbira mwa kufuna kwake osati mwa kukakamizidwa. **4)** Asakwaniritse kulumbira kwake pochita chomwe analumbira kuti sadzachita, kapena kuchisiya, chomwe analumbira kuti adzachichita. Ndipo amene walumbira nanena kuti insha Allah sikudzafunika kwa iye kulipira ngati pali zofunikira ziwiri: **A)** Kulumikiza mau oti inshaAllah ndi kulumbirako, **B)** Akhale ndi cholinga choti kulumbirako kudzachitika ngati Allah atafuna, monga kuyankhula kwake koti "ndikulumbira Allah ngati Allah atafuna".

Ndipo amene walumbira pa chinthu naona ubwino wopezeka pa chinthu chosiyana ndi chimene walumbiracho; ndiye kuti ndi Sunnat kuti alipire pa chimene walumbiracho nachita chomwe chili chabwinocho.

**DIPO LA KULUMBIRA:** Kuwadyetsa masikini khumi, ndi kum'patsa masikini aliyense chakudya cholemera (1½ kg) kapena kuwapatsa zovala, kapena kumasula kapolo, choncho amene sanapeze zimenezi, adzayenera kumanga masiku atatu motsatizana. Ndipo amene wamanga ali ndi kuthekera kodyetsa chakudya kapena kuwaveka masikini ndiye kuti ngongole yake (ya kulumbira) siinathe. Ndipo zikuloledwa kulipiliratu asanamasule kulumbirako kapena atamasula. Ndipo amene walumbira kochuluka kuposa kamodzi pa chinthu chimodzi zim'kwanira iye kulipira kamodzi, ndipo ngati zochitika zitachuluka (zolumbira) kulipiranso kudzachuluka.

✸ **MITUNDU YA MALONJEZANO: Mitundu yake:**

**1)** Kulonjeza wamba: monga kuyankhula kwa munthu konena kuti: "*Ndikadzachira ndikulonjeza kwa Allah*" ndipo wakhala chete sanalinge lonjezo lenileni ndiye kuti adzayenera kulipira kwa kulumbira kukadzapezeka kuchira. **2)** Lonjezo za kukangana ndi kupsa mtima: Komwe ndi kukuchita kulonjezako ndi chofunikira china chake ndi cholinga chofuna kukana kuchita china chake kapena pakuchita

china chake, monga kuyankhula kwa munthu konena kuti "*ngati nditayankhula nawe ndiye kuti ndidzayenera kumanga kwa chaka chathunthu*" ndipo lamulo lake ndilo asankhe pakati pa kuchita zomwe wadzipachika, kapena alipire dipo la kulumbira pa nthawi yomuyankhulitsa. **3)** Lonjezo la chinthu chololedwa: Monga kunena kuti "*Ndikulonjeza Allah kuti ndidzavala nsalu yanga*," ndipo lamulo lake ndilakuti ali ndi kusankha pakati pa kuvala nsalu kapena kupereka dipo la kulumbira. **4)** Lonjezo la chinthu chimene chili Makrooh: Monga kunena kuti "*Ndikumulonjeza Allah kuti mkazi wanga ndim'patsa chambeta*", ndipo lamulo lake ndilakuti zili Sunnat kwa iye kupereka dipo la kulumbira ndipo asachite chomwe analonjeza, ndipo ngati atachichita sadzafunika kulipira. **5)** Kulonjeza pa tchimo: Monga kunena kuti "*Ndikumulonjeza Allah kuti ndikaba*" ndipo lamulo lake ndi lakuti zili Haraam kukwaniritsa kubako, ndipo adzapereka dipo la kulumbira, ndipo ngati ataba ndiye kuti adzapeza sambi koma sadzafunika kulipira. **6)** Kulonjeza chinthu chabwino: Monga kunena kuti "*Ndikulonjeza Allah kuti ndidzaswali Swalaat yakuti*" ndi cholinga chodziyandikitsa kwa Allah. Ndipo ngati atakuchita kuswaliko chifukwa cha kuchira matenda ndiye kuti zidzakhala waajib kukwaniritsa kuswaliko ngati chitachitika chomwe amafunacho, ndipo ngati sanakuchite kuswaliko pa china chake ndiye kuti padzafunika kungokwaniritsa kuswaliko.

**KUYAMWITSA**: Zili Haraam chifukwa cha kuyamwa zomwe zili Haraam chifukwa cha ubale, ndipo zimenezo ngati pali zofunikira zitatu izi:

**1.** Ukhale mkaka wotuluka chifukwa cha kubereka koma osati pa chifukwa china.
**2.** Kuyamwa kwa khandalo kukhale mkatikati mwa zaka ziwiri zoyambirira chibadwire. **3.** Papezeke kuyamwa kasanu ndi kupitirira apo motsimikiza. Tanthauzo la kuyamwa kamodzi: ndi kuyamwa kwa mwanayo bere mpaka kulisiya berelo osati kukhuta. Sikungatsimikizike kupereka thandizo kapena kupeza gawo mu chuma chamasiye chifukwa choyamwa bere limodzi.

**WASIYA:** Zili zofunika kukwaniritsa wasiya pambuyo pomwalira mwini wasiyawo kwa amene anali ndi udindo wolongosola wasiyawo popanda umboni, choncho adzakwaniritsa wasiyawo poupereka kwa mwini wake. Ndipo wasiya uli Sunnat kwa amene wasiya chuma chambiri, choncho ndibwino kuti asiye mau opereka sadaka ndi gawo limodzi mwa magawo asanu a chuma chake kwa munthu wosauka wachibale amene sapeza nawo gawo muchuma cha masiye, ndipo ngati palibe wosauka wachibale ndiye kuti adzasiya wasiya woti sadakayo idzaperekedwe kwa masikini, Aalim, ndinso munthu wabwino. Ndipo sibwino kusiya wasiya kumunthu wosauka amene ali ndi anthu adzatenge chuma chake, pokhapokha ngati odzatenga chumawo ndi olemera ndiye kuti zikuloledwa, Ndipo zili Haraam kupereka wasiya ochuluka kupitirira pa gawo limodzi mwa magawo atatu a chuma chake (⅓) kwa munthu amene sali wachibale. Ndipo zili Haraam kupereka wasiya kwa munthu amene ali m'gulu lopeza nawo gawo kum'patsa kena kali konse ngakhale katakhala kochepa, pokhapokha ngati ataloleza abale omwe ali mgulu logawana chumacho kuti zitero pambuyo pomwalira mwini chumacho. Ndipo wasiya siudzagwira ntchito chifukwa choyankhula mwini kusiya mauwo kuti: "Ndabweza maganizo a wasiya, kapena kuti ndathetsa wasiya, kapenanso ndasintha wasiya "ndi mau ena otero. Ndipo ndibwino

kuti alembe poyamba wasiya wake kuti: Mdzina la Allah Wachisoni chambiri Wachifundo kwambiri, uwu ndiye wasiya womwe apereka iye, kuti iye akuikira umboni kuti palibe wopembedzedwa mwachoonadi koma Allah Yekha Alibe wothandizana naye, ndikutinso Muhammad (SAW) ndi Kapolo Wake komanso Mtumiki Wake, zoti kuli Jannat ndi zoona, zoti kuli moto ndi zoona, ndikutinso Kiyaamat ikubwera palibe kukaika za kubwera kwake, komanso zoti Allah adzawaukitsa anthu amene ali m'manda. Ndipo ndikupereka wasiya kwa anthu anga amene ndawasiya kuti amuope Allah ndiponso akonze chikhalidwe cha pakati pawo, ndipo ngati ali okhulupirira amumvere Allah ndi Mtumiki Wake. Ndipo ndikuwasiyira mau omwe Ibrahim ndi Ya'qoob anawalangiza ana awo onena kuti: "***E, ana anga! ndithu Allah wakusankhirani chipembedzo, choncho musamwalire pokhapokha muli Asilamu***", **(Surat 2:132)**

✸ Ndibwino ikamanenedwa swaliyatume kuphatikiza pakati pa mau oti Swalaatu ndi salaam, ndipo asangonena liwu limodzi lokha mwa mau awiriwa, ndipo chiyambireni amene sali aneneri sanenedwa kuti (SAW), choncho zisanenedwe kuti Abubakr (SAW), kapena kuti (AS), ndipo kutero ndi zoipa kwambiri, koma zikuloledwa kuphatikiza powachita amene sali aneneri otsatira kwa iwo, choncho zitha kunenedwa kuti: "E, Allah! Perekani madalitso kwa Muhammad, a ku banja la Muhammad, Maswahaaba ake, akazi ake ndi kwa ana ake."

Ndipo zili bwino kunena kuti (RA), ndinso kunena kuti Rahmatullahi alaihi kwa Maswahaaba, Matabieen ndi kwa Maulama amene anadza pambuyo pawo komanso ochita ibaadat ndi anthu ena onse omwe anali abwino, choncho zitha kunenedwa kuti Abu Hanifah, Malik, Shafi ndi Ahmad. Radhiyal-lahu anhum, kapena kunenedwa kuti Rahima humullah.

✸ **KUZINGA:** Zili waajib kuzinga nyama kuti iloledwe kuidya, ndipo choweta kuti chikhale chozingidwa pali zofunikira zingapo. **1)** Chikhale chololedwa kuchidya. **2)** Chikhale chotheka kuchizinga. **3)** Chikhale chinyamacho cha pamtunda.

**POZINGA PALI ZOFUNIKIRA ZINAYI: 1)** Wozingayo akhale wa nzeru zake (asakhale wamisala). **2)** Chida chozingira chisakhale dzino ndinso khadabo, pakuti kuzinga sikuloledwa ndi ziwirizi. **3)** Kudula kholingo lodutsa chakudya ndi lodutsa mpweya komanso misempha iwiri kapena umodzi mwa iwiriyo. **4)** Poyamba kugwedeza mkono kuti adzizinga anene mau oti ***Bismillah***, ndipo zimakhululukidwa moyiwala, n'kuthekanso kugwiritsa ntchito chiyankhulo chosakhala Charabu, ndipo ndi Sunnat ponena mau oti ***Bismillah*** kuonjezera mau oti ***Allahu Akbar***.

✸ **ULENJE: Kumeneko ndiko kusaka. Ndipo pa nyama zofunika kuzichita ulenje pali zofunikira zingapo izi:** **1)** Chikhale cha halaal kudya. **2)** Chilengedwe chake chikhale cha mtchire. **3)** Chikhale chosatheka kuchigwira.

**LAMULO LAKE:** Zikuloledwa kwa amene akufuna kuchita ulenje koma ndi makrouh kwa amene akuchita mongoseweretsa ndi mwachibwana. Ngati poulondolalondola ulenjewo uvutitse anthu, ndiye kuti uletsedwa (haraam).

**Zikuloledwa kuchita ulenje ngati pali zofunikira zinayi: 1)**Wochita ulenjeyo akhale m'gulu la omwe kuzinga kwawo n'kololedwa. **2)** Ndipo chida chozingira chikhale m'zomwe zili zololedwa kuzingira, ndipo chidacho chiyenera kukhala

chakuthwa ngati mkondo, mpaliro ndi zina zotero, ngati ulenjewo uli wochita ndi nyama yoperekera bala (yomavulaza) monga nkhwazi kapena galu ndiye kuti iyenera kukhala yophunzitsidwa. **3)**Atsimikize zakuchita ulenje komwe ndi kutumiza chida ndi cholinga cha ulenje, tsopano akapha mosafuna mwini wakeyo ndi Haraam kuchidya. **4)** Potumiza chidacho anene mau oti ***Bismillah***, ndipo apapa Tasmiyat singakhulukukidwe ngakhale ataisiya moiwala, ndipo zili Haraam kudya popanda kunenera ***Bismillah***.

✸ **CHAKUDYA:** Chimenecho ndi chilichonse chomwe chimadibwa kapena kumwedwa, ndipo chiyambi chake ndi kuloledwa kudya, choncho chakudya chilichonse n'chololedwa pakapezeka zofunikira zitatu: **1)** Chakudyacho chikhale cha Twahir. **2)** Chosapereka vuto. **3)** Chisakhale chonyansidwa nacho.

Ndipo chakudya chilichonse cha najisi chili Haraam monga magazi ndi chibudu, ndinso chomwe chingapereke vuto monga chomwe chili ndi mankhwala akupha - *poison*, komanso chonyansidwa monga mtope, mkodzo, nsabwe, ndi nsikidzi.

**NYAMA ZA PAMTUNDA ZOMWE ZILI HARAAM: 1)** Bulu wa pamudzi, zomwe zimagwira zinzake ndi mano ake monga mkango, kambuku, m'mbulu, chita, galu, nguluwe, nyani ndi chona ngakhale wa pamtunda, nkhandwe, ndi gologolo, kupatula fisi. **2)** Ndipo zili Haraam mbalame zomwe zimagwira zinzake ndi zikhadabo, monga nkhwazi, kamtema, kadzidzi ndi zina zotero, komanso zomwe zimadya zibudu monga khwangwala ndi kakowa, ndi chilichonse chomwe ma Arabu ananyansidwa nacho omwe amakhala m'mizinda monga mleme, khoswe, mavu, njuchi, ntchentche, gulugufe, ngulukulu, kanungu, ndinu ndi njoka. Komanso tizilombo monga mphutsi, mbewa, chinkankhatubzi, ndi gulo. **3)** Ndinso chilichonse chomwe shariat idalamulira kuchipha monga chinkhanira, kapena inaletsa kuchipha monga nyerere, ndi chomwe chaberekedwa pakati pa chinyama chodibwa ndi chosadibwa, monga mwana wa fisi wobadwa kuchokera mumbulu. **4)** Ndipo sichili Haraam chinyama chomwe chaberekedwa pakati pa zinyama zololedwa monga nyumbu wobadwa pakati pa bulu ndi kavalo wa m'tchire.

Ndipo zikuloledwa zosakhala zimenezi monga zifuyo ndi akavalo, ndi nyama za m'tchire monga nswala, kalulu, mbira, ntchezi, ng'azi, agwape, ndinso mbalame monga nthiwatiwa, nkhuku, peacock, njiwa, mbalame zazing'onozing'ono, bakha wa pamtunda ndi wam'madzi ndi mbalame zonse za m'madzi, komanso nyama za m'nyanja kupatula chule, njoka, ndi ng'ona. Ndipo ndiwo ndi zipatso zomwe zathiriridwa kapena kuthiridwa manyowa anyansi zikuloledwa kuzidya pokhapokha ngati kutaonekera kukoma kwa najisi kapena fungo lake m'menemo ndiye kuti zili Haraam kudya. Ndi makrooh kudya makala, dothi ndi dongo,tsono anyezi, adiyo ndi zina zotero (zafungo) pokhapokha ataziphika, koma ngati itam'peza njala ndipo wasimidwa adzayenera kudya zongotseka njala yake basi.

✸ Ndi Haraam kuwafunira mafuno abwino makafiri pa zisangalalo zawo kapena kukhala nawo pa zisangalalozo, kuyambiza kuwapatsa salaam, ndipo ngati atayambiza kutipatsa salaam zifunika kuwabwezera ndi mau onena kuti wa alaikum. Ndipo zili Haraam kuimirira chifukwa cha kubwera kwao komanso kuimirira chifukwa cha munthu wa bidah, ndiponso sibwino kugwirana nawo chanza. Koma kuwapepesa ndi kukawazonda akadwala zili Haraam pokhapokha ngati pali ubwino wovomerezeka pa shariat.

# MADUAA A SHARIAT

Ndithu wolingalira m'machitidwe a Allah akudziwa kuti mavuto ndi njira imodzi mwa njira Zake za chikonzero cha dziko lapansi. Allah akunena kuti: "*Ndipo tikuyesani ndi mantha (monga nkhondo), njala, kuchepa kwa chuma, kutaika kwa miyoyo ndi kuonongeka kwa mbeu. Choncho auze nkhani yabwino opirira*" **(Surat 2:155).** Ndipo akulakwitsa amene akuganiza kuti anthu ochita zabwino ali kutali ndi mavuto, koma kuti mavuto ndi chisonyezo cha Imaan. Tsiku lina Mtumiki (SAW) anafunsidwa kuti ndi ndani mwa anthu amene amapeza mavuto kwambiri, Mtumiki (SAW) poyankha anati: "*Aneneri, kenako anthu ochita zabwino, kenako anthu ofanana ndi iwo, munthu amapatsidwa mavuto molingana ndi Deen yake, choncho ngati ali wolimba mu Deen yake ndiye kuti mavuto ake amaonjezereka, ndipo ngati ali wofewa pa Deen yake ndiye kuti amapeputsidwa mavuto kwa iye.*" **(Ibn Maajah.)** Ndipo mavutowo ndi chimodzi mwa zizindikiro za chikondi cha Allah kwa kapolo Wake, Mtumiki (SAW) anati: "*Ndithu Allah akawakonda anthu ena ake amawapatsa mavuto*". **(Ahmad),** ndipo chimodzi mwa zizindikiro kuti Allah akumufunira zabwino kapolo Wake, Mtumiki (SAW) anati: "*Allah akamufunira zabwino kapolo Wake amam'patsiratu vuto pa dziko lino lapansi, ndipo Allah akamufunira zoipa kapolo Wake amamulekerera pa tchimo lomwe wachita kuti adzalipidwe ndi tchimo limenelo pa tsiku la Kiyaamat.*" **(Tirmidh)** Ndipo vutolo limafafaniza machimo ngakhale litachepa. Mtumiki (SAW) anati: "*Palibe Msilamu aliyense amene lingam'peze vuto la minga ndi chochepera pa mingapo koma kuti Allah amam'fafanizira tchimolo ndi vutolo monga momwe mtengo umagwetsera masamba ake.*" **(Bukhaari, Muslim)** . Ndipo pa chifukwa chimenecho Msilamu amene ali pa vuto ngati ali wochita zabwino ndiye kuti vutolo limafafaniza machimo amene anachita kale, kapena kutukula ulemerero wake, ndipo ngati anali wonyozera malamulo ndiye kuti vutolo limafafaniza machimo, komanso limankumbutsa kuopsa kwa machimowo. Allah akunena kuti: "*Kuononga kwaonekera pamtunda ndi panyanja chifukwa cha zomwe manja a anthu achita, kuti awalawitse zina zomwe achita kuti mwina angabwerere (kuchita toba)*".

**MITUNDU YA MAYESERO:** Mayesero kudzera mu mtendere; monga kuonjezereka kwa chuma, ndi mayesero kudzera mu zowawa; monga mantha a nkhondo, njala ndi kupunguka kwa chuma. Allah akunena kuti "*Ndipo tikuyesani kudzera mu chowawa ndi chabwino kukhala mayesero*". Ndipo mtundu wina ndi mayesero kudzera m'matenda ndi imfa omwe chifukwa chake chachikulu ndi diso loipa komanso matsenga zochitika chifukwa cha kaduka, Mtumiki (SAW) ananena kuti "*Ambiri amene amamwalira mu Ummat wanga pambuyo pa chigamulo cha Allah ndi chikonzero Chake ndi chifukwa cha diso loipa*" **(Al-Twayaalisiyy).**

**KUDZITCHINJIRIZA KU DISO LOIPA KOMANSO KU MATSENGA**

Kudzitchinjiriza kuli bwino kusiyana ndi kuchiza, choncho zifunika ife kuti tiyesetse kudzitchinjiriza. Ndipo njira zina zazikuluzikulu zodzitchinjirizira ndi izi:

✸ Kuulimbikitsa moyo ndi Tauheed, kukhulupilira kuti woyendetsa dziko ndiye Allah ndi kuchulutsa kuchita zabwino. ✸ Kumuganizira zabwino Allah ndi kuyedzamira kwa Iye, choncho asawaganizire matenda kapena diso loipa kuti zachitika chifukwa cha china chake, pakuti kuganizirako pakokha ndi matenda.

✸ Ndipo zikatchuka za munthu wina kuti iye ndi wa diso loipa kapena wamatsenga ndiye kuti munthu ameneyo apewedwe komwe kuli njira imodzi yopewera simantha ayi. ✸ Kumutchula Allah ndi kufuna madalitso akachiona chomwe chikumusangalatsa, Mtumiki (SAW) anati; "*Mmodzi wa inu akadziona iye mwini kapena chuma chake, kapena mwa m'bale wake chomwe akuchikonda, apemphe madalitso, pakuti zoti kuli diso loipa n'zoona*" **(Haakim).** Kuyankhula kuti: '***Baaraka Allah laka'*** osati: 'tabaaraka Allah'. ✸ Ndipo njira zina zopewera ku matsenga ndiye kudya m'mawam'mawa tende musanu ndi muwiri wa aj'wa ochokera ku Madinat Munawwarat. ✸ Kuthawira kwa Allah, kuyedzamira mwa Iye, kumuganizira zabwino, kudzitchinjiriza ndi Iye ku diso loipa ndi ku matsenga, ndi kumawerenga nthawi zonse ma Zikr, ndi kudzitchinjiriza tsiku lililonse m'mawa ndi madzulo. Ndipo ma Duaa amenewa ali ndi mphamvu, imaonjezereka ndi kupungula ndi chifuniro cha Allah pa zinthu ziwiri: **1)** Kukhulupirira kuti zomwe zadza m'ma Duaamo ndi zenizeni komanso zoona, ndikutinso zimathandiza kudzera mu chifuniro cha Allah. **2)** Lirime lake liyankhule ponena ma Duaawo, ndipo makutu ake amvetsere, komanso mtima wake ukhale uli pompo, chifukwa imeneyi ndi Duaa, ndipo Duaa simayankhidwa yochokera mu mtima wosalabadira wamasewera, monga zinatsimikizika kuchokera kwa Mtumiki (SAW).

**NTHAWI YOCHITIRA DUAA NDI KUDZITCHINJIRIZA:** MaDuaa a m'mawa adzinenedwa pambuyo pa Swalaat ya Fajr, tsopano ma Duaa a madzulo amenewo adzinenedwa pambuyo pa Swalaat ya Asr, ndipo Msilamu ngati waiwala kuwanena ma Duaa wo, kapena sanalabadire ndiye kuti awanene nthawi imene awakumbukire.

**ZIZINDIKIRO ZA KUGWIDWA NDI DISO LOIPA NDI ZINA ZOTERO:** Palibe kutsutsana pakati pa udotolo ndi ma Duaa ovomerezeka ndi shariat, pakuti mu Qur'an muli machiritso a matenda a ziwalo ndi a uzimu. Ndipo munthu akakhala kuti ali bwinobwino ku matenda a ziwalo ndiye kuti zomupeza kawirikawiri zimakhala ngati kupweteka kwa mutu, kuonekera chikasu kunkhope, kutuluka thukuta kwambiri komanso kukodza kwambiri, kufooka kwa chilakolako cha chakudya, kunjenjemera zala, kapena kumva kutentha, kapena kuzizira mu nsonga, kumva kunjenjemera mu mtima, kumva kuwawa kuchokera kunsi kwa msana ndi mapewa awiri, kudandaula komanso kubanika m'chifuwa, kusowa tulo ta usiku, kudzidzimuka koopsa chifukwa cha mantha ndi ukali wosakhala wa chilengedwe, kugeyageya, kuwusa mtima, kukonda kudzipatula, kufooka ndikumva ulesi, kukonda kugona, ndi mavuto ena a umoyo opanda chifukwa cha udotolo. Ndipo zizindikiro zimenezi kapena zina mwa izo zimapezeka molingana ndi mphamvu ya matenda kapena kufooka kwake. Ndipo ndi zofunikira kwa Msilamu kuti Imaan ndi mtima wake zikhale zolimba, osalowamo manong'onong'o. Choncho asadziganizire kuti wagwida ndi matenda chifukwa chongomva chimodzi mwa zizindikiro zimenezi, chifukwa kuganizira ndi matenda ovuta kuwachiza. Ndipo zina mwa zizindikirozi zimatha kupezeka kwa ena chikhalirecho iwo ndi angwiro, ndiponso nthawi zina zimatha kupezeka ndikukhala chifukwa cha matenda a chiwalo, ndipo nthawi zina chifukwa chake chimakhala chifukwa cha kufooka Imaan, monga kubanika kwa chifuwa, kudandaula, kufooka m'thupi, choncho ayenera kuuyang'anitsitsa mgwirizano wake ndi Allah.

**Tsono matenda akakhala chifukwa cha diso loipa ndiye kuti machiritso ake mu kufuna kwa Allah adzakhala ndi chimodzi mwa zinthu ziwiri: 1)** Ngati wamudziwa mwini diso loipalo: Umulamule kuti asambe, ndipo utenge madzi amenewo kapena utenge zotsalira zake monga chakudya chake kapena chakumwa chake kenako usambe ndi kumwa. **2)** Ngati sanadziwike mwini diso loipalo ndiye kuti kuchilitsa kwake kudzakhala ndi ruqyat, Duaa ndi chiuwi (kudula litsipa).

**Tsopano akakhala matendawo chifukwa cha matsenga ndiye kuti mukufuna kwa Allah kuchiritsa kwake kudzakhala ndi chimodzi mwa zinthu zingapo izi: 1)** Awadziwe malo wochitira matsenga: Choncho akachipeza chomwe achitira matsengacho amasule mfundo zake akuwerenga Surat Falaq komanso Nas, kenako achiotche. **2)** MaDuaa ovomerezeka mu shariat: Ndi ma Ayat a Qur'an, kwenikweni ndi Surat Nas, Falaq komanso ndi Baqarat ndi maDuaa, posachedwa zibwera zimenezi. **3)** Kutsirikula: Nako kuli mitundu iwiri: **A)** Kwa Haraam komwe ndi kutsirikula matsenga kudzera m'matsenga, ndi kuwapitira amatsenga kuti atsirikule. **B)** Kovomerezeka: Ndiko kwina mwa iko ndikutenga masamba asanu ndi awiri a msau ndikuwasinja, kenako nkuwawerengera Surat Kafiroon, Ikhlas, Falaq ndi Nas, katatukatatu, kenako nkuwaika m'madzi, keneko n'kusamba ndikumamwa madzi amenewo, ndikumabwereza kuchita zimenezo mpaka kuchira insha Allah. **(AbdulRazzaqq).** **4)** Kuchotsa ufiti: Kuthira zomwe zingatsegule m'mimba ngati ufitiwo uli m'mimbamo, ndi kuwuwika ngati suli m'mimba.

**RUQYAT (DUWA):**

**Zofunikira zake: 1)** Ikhale ya ma Ayat a Qur'an ndi ma Duaa ovomerezeka ndi shariat. **2)** Ikhale ya m'chiyankhulo cha Charabu, koma ma Duaa akuloledwa m'chiyankhulo china. **3)** Kukhulupirira kuti ruqyat payokha ilibe mphamvu, ndikuti machilitso amachokera kwa Allah. ndipo poonjezera mphamvu ya ruqyat ayenera kuwerenga Qur'an ndi Niyyat ya machiritso komanso chiongoko kwa anthu ndi majini, pakuti Quran inavumbulutsidwa kukhala chiongoko komanso machilitso, ndipo asaiwerenge Qur'aniyo ndi cholinga cha kupha majini pokhapokha ngati litavuta kutuluka kwake Jinilo ndi zomwe zanenedwa zija.

**ZOFUNIKIRA ZA WOCHITA RUQYAT: 1)** Akhale Msilamu, ndiponso akhale wochita zabwino wa Taqwa, nthawi iliyonse akakhala womuopa Allah kwambiri ruqyat imakhala yamphamvu kwambiri. **2)** Atembenukire kwa Allah mwachoonadi mkatikati mochita ruqyat, kotero kuti mtima ndi lirime zikhale pamodzi, ndi bwino kwambiri kuti munthu adzichitire ruqyatyo yekha, chifukwa choti kawirikawiri wapadera mtima wake umakhala wotanganidwa, chifukwanso choti palibe wofanana naye yemwe akumva kupanikizikako ndi kufunika kwake, ndipo anthu amene ali pa mpanipani Allah awalonjeza za kulandiridwa pempho lawo.

**ZOFUNIKIRA ZA MUNTHU WOCHITIRIDWA RUQYAT: 1)** Ndibwino kuti akhale wokhulupirira wabwino, ndi m'mene chikhulupiriro chingakulire ndi m'menenso magwiridwe a ntchito amakulira, Allah akunena kuti "*Ndipo tikuvumbulutsa Qur'an yomwe imachiritsa matenda a m'mitima ndiponso ndi chifundo kwa okhulupirira. Komabe osalungama sikuwaonjezera kanthu kena koma kutaika* **(Surat 17:82)**. **2)** Kutembenukira kwa Allah mwachoonadi kuti

amuchilitse. **3)** Asaone kuchedwa kuchira chifukwa choti ruqyat ndi Duaa, ndipo akafunitsitsa kuyankhidwa mwa msanga nkutheka osayankhidwa, Mtumiki (SAW) anati "*Amayankhidwa mmodzi wa inu pempho lake ngati sanachite changu, amanena kuti ndapempha koma sindinayankhidwe*" (Bukhaari, Muslim) .

**KUPEMPHERERA KULI NDI NJIRA ZINGAPO**: **1)** Kuwerenga Duaa ya machiritso ndi kulavula timalovu. **2)** Kuwerenga mosalavulira timalovu. **3)** Kutenga malovu ndi chala ndikuwasakaniza ndi dothi ndikuwapaka pa malo womwe akupweteka. **4)** Kuwerenga Duaa ya machiritso nkumasisita malo womwe akupwetekawo.

**MA AYAT NDI MA HADITH OGWIRITSIDWA NTCHITO POMUPEMPHERERA WODWALA**: Surat Faatihat, Ayatul kursi, ma Ayat awiri omalizira amu Surat Baqqrah, ma surat a Kafiroon, Ikhlaas, Falaq ndi Nas, surat

Ma ayat ndi mahadith omuchitira ruqyat munthu wodwala:

Suurat –ul Faatihat, Aayatul Kursiyy, ma ayat awiri a mapeto a Suurat-ul-Baqarat, Suurat-ul-Kaafiruun, Suutat-ul-Ikhlaas, Suurat-ul-Falaq, Suurat-ul Naas ndi ma ayat awa:

﴿ ٱللَّهُ لَآ إِلَٰهَ إِلَّا هُوَ ٱلْحَىُّ ٱلْقَيُّومُ ۚ لَا تَأْخُذُهُۥ سِنَةٌ وَلَا نَوْمٌ ۚ لَّهُۥ مَا فِى ٱلسَّمَٰوَٰتِ وَمَا فِى ٱلْأَرْضِ ۗ مَن ذَا ٱلَّذِى يَشْفَعُ عِندَهُۥٓ
إِلَّا بِإِذْنِهِۦ ۚ يَعْلَمُ مَا بَيْنَ أَيْدِيهِمْ وَمَا خَلْفَهُمْ ۖ وَلَا يُحِيطُونَ بِشَىْءٍ مِّنْ عِلْمِهِۦٓ إِلَّا بِمَا شَآءَ ۚ وَسِعَ كُرْسِيُّهُ ٱلسَّمَٰوَٰتِ وَٱلْأَرْضَ ۖ
وَلَا يَـُٔودُهُۥ حِفْظُهُمَا ۚ وَهُوَ ٱلْعَلِىُّ ٱلْعَظِيمُ ﴾[1]

﴿ ءَامَنَ ٱلرَّسُولُ بِمَآ أُنزِلَ إِلَيْهِ مِن رَّبِّهِۦ وَٱلْمُؤْمِنُونَ ۚ كُلٌّ ءَامَنَ بِٱللَّهِ وَمَلَٰٓئِكَتِهِۦ وَكُتُبِهِۦ وَرُسُلِهِۦ لَا نُفَرِّقُ بَيْنَ أَحَدٍ مِّن
رُّسُلِهِۦ ۚ وَقَالُوا۟ سَمِعْنَا وَأَطَعْنَا ۖ غُفْرَانَكَ رَبَّنَا وَإِلَيْكَ ٱلْمَصِيرُ ﴿٢٨٥﴾ لَا يُكَلِّفُ ٱللَّهُ نَفْسًا إِلَّا وُسْعَهَا ۚ لَهَا مَا كَسَبَتْ
وَعَلَيْهَا مَا ٱكْتَسَبَتْ ۗ رَبَّنَا لَا تُؤَاخِذْنَآ إِن نَّسِينَآ أَوْ أَخْطَأْنَا ۚ رَبَّنَا وَلَا تَحْمِلْ عَلَيْنَآ إِصْرًا كَمَا حَمَلْتَهُۥ عَلَى ٱلَّذِينَ مِن
قَبْلِنَا ۚ رَبَّنَا وَلَا تُحَمِّلْنَا مَا لَا طَاقَةَ لَنَا بِهِۦ ۖ وَٱعْفُ عَنَّا وَٱغْفِرْ لَنَا وَٱرْحَمْنَآ ۚ أَنتَ مَوْلَىٰنَا فَٱنصُرْنَا عَلَى ٱلْقَوْمِ ٱلْكَٰفِرِينَ ﴾[2]

[3]﴿ فَسَيَكْفِيكَهُمُ ٱللَّهُ ۚ وَهُوَ ٱلسَّمِيعُ ٱلْعَلِيمُ ﴾

[4]﴿ يَٰقَوْمَنَآ أَجِيبُوا۟ دَاعِىَ ٱللَّهِ وَءَامِنُوا۟ بِهِۦ يَغْفِرْ لَكُم مِّن ذُنُوبِكُمْ وَيُجِرْكُم مِّنْ عَذَابٍ أَلِيمٍ ﴾

[5]﴿ وَنُنَزِّلُ مِنَ ٱلْقُرْءَانِ مَا هُوَ شِفَآءٌ وَرَحْمَةٌ لِّلْمُؤْمِنِينَ ۙ وَلَا يَزِيدُ ٱلظَّٰلِمِينَ إِلَّا خَسَارًا ﴾

[7]﴿ وَإِذَا مَرِضْتُ فَهُوَ يَشْفِينِ ﴾ [6]﴿ أَمْ يَحْسُدُونَ ٱلنَّاسَ عَلَىٰ مَآ ءَاتَىٰهُمُ ٱللَّهُ مِن فَضْلِهِۦ ﴾

[9]﴿ قُلْ هُوَ لِلَّذِينَ ءَامَنُوا۟ هُدًى وَشِفَآءٌ ﴾ [8]﴿ وَيَشْفِ صُدُورَ قَوْمٍ مُّؤْمِنِينَ ﴾

[1]﴿ فَٱرْجِعِ ٱلْبَصَرَ هَلْ تَرَىٰ مِن فُطُورٍ ﴾ [10]﴿ لَوْ أَنزَلْنَا هَٰذَا ٱلْقُرْءَانَ عَلَىٰ جَبَلٍ لَّرَأَيْتَهُۥ خَٰشِعًا مُّتَصَدِّعًا مِّنْ خَشْيَةِ ٱللَّهِ ﴾[1]

---

[1] 2:255.

[2] 2: 285/286.

[3] "Ndipo Allah adzakukwaniritsira (za masautso awo) poti Iye Ngwakumva, Ngodziwa." (2: 137)

[4] "Eh inu anthu athu! Muyankheni woitana wa Allah ndiponso m'khulupirireni, akukhululukirani (Allah) ena mwa machimo anu komanso akupulumutsani ku chilango chopweteka". (46: 32)

[5] "Ndipo timatumiza kuchokera mu Qur'aan chomwe ndi machiritso ndi chifundo kwa anthu okhulupirira ndipo sichimawaonjezera anthu opondereza kena kake kupatula chitaiko". (17: 82)

[6] "Kapena akuwachitira anthu njiru pa zomwe Allah wawapatsa mu zabwino Zake". (4: 54)

[7] "Ndipo ine ndikadwala Iye (Allah) amandichiritsa". (26: 80)

[8] "Ndipo Iye (Allah) amachiritsa zifuwa za anthu okhulupirira". (9: 14)

[9] "Nena: zimenezi ndi za anthu okhulupirira, chiongolo komanso machiritso". (41: 44)

[10] "Tikadavumbulutsira Qur'aan imeneyi pa phiri bwenzi utaliona likudzichepetsa mosweka chifukwa choopa Allah". (59: 21)

[2]﴿وَإِن يَكَادُ ٱلَّذِينَ كَفَرُواْ لَيُزْلِقُونَكَ بِأَبْصَٰرِهِمْ لَمَّا سَمِعُواْ ٱلذِّكْرَ وَيَقُولُونَ إِنَّهُۥ لَمَجْنُونٌ﴾
﴿وَأَوْحَيْنَآ إِلَىٰ مُوسَىٰٓ أَنْ أَلْقِ عَصَاكَ فَإِذَا هِىَ تَلْقَفُ مَا يَأْفِكُونَ ﴿١١٧﴾ فَوَقَعَ ٱلْحَقُّ وَبَطَلَ مَا كَانُواْ يَعْمَلُونَ ﴿١١٨﴾ فَغُلِبُواْ
هُنَالِكَ وَٱنقَلَبُواْ صَٰغِرِينَ﴾[3]
﴿قَالُواْ يَٰمُوسَىٰٓ إِمَّآ أَن تُلْقِىَ وَإِمَّآ أَن نَّكُونَ أَوَّلَ مَنْ أَلْقَىٰ ﴿٦٥﴾ قَالَ بَلْ أَلْقُواْ فَإِذَا حِبَالُهُمْ وَعِصِيُّهُمْ يُخَيَّلُ إِلَيْهِ مِن
سِحْرِهِمْ أَنَّهَا تَسْعَىٰ ﴿٦٦﴾ فَأَوْجَسَ فِى نَفْسِهِۦ خِيفَةً مُّوسَىٰ ﴿٦٧﴾ قُلْنَا لَا تَخَفْ إِنَّكَ أَنتَ ٱلْأَعْلَىٰ ﴿٦٨﴾ وَأَلْقِ مَا فِى
يَمِينِكَ تَلْقَفْ مَا صَنَعُوٓاْ إِنَّمَا صَنَعُواْ كَيْدُ سَٰحِرٍ وَلَا يُفْلِحُ ٱلسَّاحِرُ حَيْثُ أَتَىٰ﴾[4]
[5]﴿ثُمَّ أَنزَلَ ٱللَّهُ سَكِينَتَهُۥ عَلَىٰ رَسُولِهِۦ وَعَلَى ٱلْمُؤْمِنِينَ﴾
[6]﴿فَأَنزَلَ ٱللَّهُ سَكِينَتَهُۥ عَلَيْهِ وَأَيَّدَهُۥ بِجُنُودٍ لَّمْ تَرَوْهَا﴾
[7]﴿فَأَنزَلَ ٱللَّهُ سَكِينَتَهُۥ عَلَىٰ رَسُولِهِۦ وَعَلَى ٱلْمُؤْمِنِينَ وَأَلْزَمَهُمْ كَلِمَةَ ٱلتَّقْوَىٰ﴾
[8]﴿لَّقَدْ رَضِىَ ٱللَّهُ عَنِ ٱلْمُؤْمِنِينَ إِذْ يُبَايِعُونَكَ تَحْتَ ٱلشَّجَرَةِ فَعَلِمَ مَا فِى قُلُوبِهِمْ فَأَنزَلَ ٱلسَّكِينَةَ عَلَيْهِمْ وَأَثَٰبَهُمْ فَتْحًا قَرِيبًا﴾
[9]﴿هُوَ ٱلَّذِىٓ أَنزَلَ ٱلسَّكِينَةَ فِى قُلُوبِ ٱلْمُؤْمِنِينَ لِيَزْدَادُوٓاْ إِيمَٰنًا مَّعَ إِيمَٰنِهِمْ﴾

## Ndipo ma Hadith:

- أَسْأَلُ اللهَ العَظِيمَ رَبَّ العَرْشِ العَظِيْمِ أَنْ يَشْفِيَكَ (kasanu ndi kawiri).[10]
- أُعِيْذُكَ بِكَلِمَاتِ اللهِ التَّامَةِ مِنْ كُلِّ شَيْطَانٍ وَهَامَّةٍ وَمِنْ كُلِّ عَيْنٍ لامَّةٍ (katatu).[11]
- اللَّهُمَّ رَبَّ النَّاسِ أَذْهِبِ البَأْسِ وَاشْفِ أَنْتَ الشَّافِي لا شِفَاءَ إلا شِفَاؤُكَ شِفَاءً لا يُغَادِرُ سَقَمًا (katatu).[12]
- اللَّهُمَّ أَذْهِبْ عَنْهُ حَرَّهَا وَبَرْدَهَا وَوَصَبَهَا (kamodzi).[13]

---

[1] "Ndipo bwezeretsanso kuyang'ana kodi ukuonako mung'alu?" (67: 3)

[2] "Ndipo makafiri adayandikira kukugwetsa iwe (Muhammad SAW) ndi maso awo pamene adachimva chikumbutsochi (Qur'aan) ndipo akumanena ndithu iyeyu ndi wamisala". (68: 51)

[3] "117 Ndipo tidavumbulutsa kwa Mussa (AS) kuti ponya ndodo yakoyo tero idayamba kumeza zimene adazipekazo 118 Ndipo choonadi chidapezeka ndipo zidawonongeka zomwe iwo adali kuzichita." 119 Ndipo adagonjetsedwa kumeneko nabwerera ali onyozeka" (7: 117-119)

[4] 65 Ndipo iwo adati: "Eh iwe Mussa (AS)! Kodi uti uponye ndi iwe kapena tikhale ife oyamba amene ati aponye? 66 Iye (Mussa AS) adati: 'Koma ponyani', nthawi yomweyo zingwe komanso ndodo zawo zidayamba kuoneka kwa iye ngati kuti zikuyenda 67 Ndipo mu mtima mwake, Mussa (AS) mudachita mantha 68 Tidanena Ife kuti: "Usaope ndithudi iweyo ndiwe wapamwamba 69 Ndipo ponya chomwe chili kumanja kwako chimeza zomwe apanga, ndithudi zimene iwo apanga ndi ndale za afiti ndipo mfiti siingapambane paliponse ingapite." (20:65-69)

[5] "Kenako Allah adatsitsa chidekherero Chake pa Mtumiki (SAW) Wake komanso pa anthu okhulupirira" (9:26)

[6] "Ndipo Allah adatsitsa chidekherero Chake pa iye (Mtumiki SAW) ndipo adamuthangatira ndi asirikali amene simudawaone". (9:40)

[7] "Ndipo Allah adatsitsa chidekherero Chake pa Mtumiki (SAW) Wake komanso pa anthu okhulupirira ndi kuwapatsa liwu loopa (Allah)." (48:26)

[8] "Ndithudi Allah wasangalala nawo anthu okhulupirira pamene adali kukuvotera iwe (Mtumiki SAW za imfa) pansi pa mtengo tero (Allah) adatulutsira poyera zomwe zidali m'mitima mwawo ndipo adatsitsa chidekherero pa iwo ndiponso adawalipira chigonjetso chapafupi." (48:18)

[9] "Iye ndi Amene adatsitsa chidekherero m'mitima mwa anthu okhulupirira kuti awonjezereke chikhulupiriro pamodzi ndi chikhulupiriro chawo" (48:4)

[10] "Ndikum'pempha Allah Wolemekezeka Mwini mpando wachifumu wolemekezeka kuti akuchilitse"

[11] "Ndikukutchinjiriza ndi mau a Allah okwanira ku Satana aliyense, zoipa zilizonse ndi kudiso lililonse loipa"

[12] "E, Allah! Mbuye wa anthu chotsani vuto, chiritsani, pakuti Ndinu Wochiritsa, palibe machiritso ochokera kwa wina koma machiritso Anu, machiritso osasiya matenda"

[13] "E, Allah! mchotsereni kutentha kwake, kuzizira kwake ndi kupweteka kwake"

- حَسْبِيَ اللهُ لا إِلَهَ إِلا هُوْ عَلَيْهِ تَوَكَّلْتُ وَهُوَ رَبُّ العَرْشِ العَظِيْمِ (kasanu ndi kawiri).[1]
- بِسْمِ اللهِ أَرْقِيْكَ مِنْ كُلِّ دَاءٍ يُؤْذِيْكَ وَمِنْ شَرِّ كُلِّ نَفْسٍ أَوْ عَيْنِ حَاسِدٍ، اللهُ يَشْفِيْكِ بِسْمِ اللهِ أَرْقِيْكَ (katatu).[2]
- **Uyike dzanja lako pamene pakuwawa ndipo unene kuti:** بِسْمِ اللهِ "*Mdzina la Allah*" (katatu) أَعُوْذُ بِعِزَّةِ اللهِ وَقُدْرَتِهِ مِنْ شَرِّ مَا أَجِدُ وَأُحَاذِرُ (kasanu ndi kawiri).[3]

**MACHENJEZO**

**1.** Sizikuloledwa kuvomereza mabodza a munthu wochiza matenda a diso loipa monga kumwa mkodzo wake, ndikuti mphamvu yake sipindula akazindikira.

**2.** Sizololedwa kuvala zithumwa monga zikopa, zibangiri ndi mikanda poopa kumgwera diso loipa, Mtumiki (SAW) anati: "*Amene angadzipachike china chake adzamusiyira chimenecho kuti chimuthandize* (Tirmidhi), ndipo chinthucho ngati chili chochokera mu Qur'an pamenepo pali kusiyana maganizo a Maulama, koma kuzisiya ndibwino.

**3.** Kulemba mau oti ma sha Allah Tabarakaatllah, kapena kujambula lupanga, kapena mpeni, kapena diso, kapena kuika Quran mgalimoto, kapena kupachika mnyumba ma Ayat ena, zonsezo sizitchinjiriza ku diso loipa, koma zitha kukhala m'matalasimu a Haraam.

**4.** Zifunika kuti munthu wodwala atsimikize za kuyankhidwa, ndipo asaone kuchedwa kuchira, pakuti akauzidwa kuti kuchiritsidwa ndi mankhwala kumatenga moyo onse sakhumudwa, koma iye amakhumudwa pemphero la matenda ake likatalika, chikhalilecho iye amapeza sawabu pa chilembo chilichonse chimene akuchiwerenga, ndipo pa sawabu iliyonse amalipidwa sawabu zonga imeneyo zokwanira khumi, ndipo ayenera kumachita Duaa, kuchita Istighfaar ndinso kuchulutsa kupereka sadaka, pakuti zimenezi ndi zina mwa zimene munthu amachilitsidwa nazo.

**5.** Kuwerenga Qur'an pa gulu n'kosemphana ndi Sunnat, ndipo Hadith yonena zimenezo ndi yofooka, chimodzimodzinso kungogwiritsira ntchito Tape Recorder wotola mawu pakuti m'menemo simumapezekamo Niyyat pomwe Niyyatyo ndi yofunikira kwa amene akuchita pemphero lochiza matenda ngakhale kuti kumverera kwake kuli ndi ubwino.Ndipo ndi Sunnat kubwerezabwereza pemphero kwa munthu wodwala mpaka atachiritsidwa pokhapokha ngati kukumtopetsa ndiye kuti adzachepetsa kuti asatope. Tsopano kubwerezabwereza Ayat ndi Duaa ndi chiwerengero chapadera sizoona pokhapokha ngati pali umboni.

**6.** Pali zizindikiro zosonyeza umboni kapena mbali yake ina, kuti wopempherayo akugwiritsa ntchito matsenga osati Qur'an, ndipo zisakunyenge zina zomwe iye amaonetsa kuchokera mu Deen, pakuti nthawi zina amatha kuyamba kuwerenga kwake ndi Qur'an ndipo sakhala nthawi amazitembenuza zimenezo, ndipo nthawi zina amakhala wa ena omwe anazolowera kukhala m'mizikiti pofuna kuwanamiza

---

[1] "Wandikwanira Allah, palibe wopembedzedwa mwachoonadi koma Iye, ndayedzamira kwa Iye, ndipo Iye ndi Mwini mpando wachifumu wolemekezeka"

[2] "Mdzina la Allah ndikukupempherera ku matenda alionse omwe akukuvuta iwe, ndi ku zoipa za munthu aliyense, kapena diso la munthu wakaduka, Allah akuchiritse, mdzina la Allah ndikukupemphelera"

[3] ndikudzitchinjiriza ndi ulemerero wa Allah ndi mphamvu Yake ku zowawa zomwe ndi kumva ndi kuziona.

anthu, ndipo nthawi zina udzamuona akuchulutsa kuchita Zikr pamaso pako, choncho zisakunyenge zimenezi, tero uchenjere.

**ZINA MWA ZIZINDIKIRO ZA ANTHU A MATSENGA NDI A MIZIMU**

✸ Kumufunsa wodwala dzina lake kapena dzina la amayi ake, chifukwa kulidziwa dzina kapena kusalidziwa sikumasintha kalikonse popereka mankhwala. ✸Kuitanitsa kena kake mu zovala za wodwala, monga nsalu kapena kachitambaya. ✸ Nthawi zina amaitanitsa kuchokera kwa wodwala nyama ya maonekedwe apadera kuti akachizingire chiwanda, ndipo nthawi zina amatha kumpaka wodwalayo magazi a nyamayo. ✸ Kulemba kapena kuwerenga matalasimu omwe sali omveka komanso alibe tanthauzo. ✸ Kum'patsa wodwala pepala lolembedwa mkati mwake timabokosi momwe muli zilembo ndi manambala, ndipo zimatchedwa kuti "tchinjirizo". ✸ Kumulamula wodwala kudzipatula kwa anthu mu kanthawi kochepa ndi kukhala mchipinda momwe muli mdima, ndipo zimatchedwa kuti AlHajjabatu. ✸ Kumulamula wodwala kuti asakhudze madzi kwa kanthawi kodziwika. ✸ Kum'patsa wodwala chinthu china chake kuti akachikwirire m'nthaka, kapena pepala kuti akaliotche ndi kudzifukitsira nalo. ✸ Kumuuza wodwala zina za iye zomwe sangazidziwe wina, kapena kumuuza dzina lake, mudzi wake ndi matenda ake asanayankhule. ✸ Kupima momwe wodwala alili chongolowa kwa iye, kapena ndi phone, kapenanso ndi kalata yotumizidwa.

**7.** Mazhab a Ahlus-sunnat akunena kuti chiwanda chimasakanikirana ndi munthu, ndipo umboni wake ndi mau a Allah onena kuti: "*Amene akudya chuma cha katapira sadzauka m'manda koma monga momwe amaimirira munthu wokhudzidwa ndi ziwanda, mwa misala*." **(Surat 2:275)**. Ndipo akuluakulu a Tafseer anagwirizana kuti tanthauzo la kukhudzidwa mu Ayat imeneyi ndi misala ya chisatana yomwe imamupeza munthu chifukwa cha kusakanikirana chiwanda ndi iye.

**KUTSENDERA: UFITI:** Ufiti ulipo ndipo zotsatira zake ndizotsimikizika ndi Quran komanso Hadith. Ufitiwo ndi haraam komanso ndi tchimo lalikulu kwambiri chifukwa chakuyankhula kwa Mtumiki (SAW) kwakuti: "Pewani machimo asanu ndi awiri odzetsa munthu kuchiononongeko, (maswahaaba) adati: 'Ndi ati machimo amenewo iwe Mtumiki wa Allah?' Iye adati: *"kuphatikiza Allah ndi zinthu zina zake pom'pembedza (shirk), ufiti........."* **(Bukhaari Muslim)**. Komanso kuyankhula kwa Allah (SW) kwakuti: *"Ndithudi iwo akudziwa kwa munthu amene waugula (ufiti) alibe pa tsiku lomaliza pokakhala paliponse pabwino."*

**ufitiwo uli m'magawo awiri: 1)** Fundo ndi mapemphero – matemberero – amene amafika nawo kudzera mwa iwo mfiti kugwiritsira ntchito a satana mu zomwe akufuna kuvutitsa nazo wolodzedwayo. **2)** Mankhwala amene amachita kanthu pa thupi la wolodzedwa, nzeru zake, khumbo lake ndi kupendekera kwake. Uwu umatchedwa mlekanitso ndi khudzumule (kondaine). Ndiye zimaganiziridwa kwa wolodzedwayo ngati kuti chinthu ichi chatembenuka ndipo ichi chatekeseka kapena chayenda ndi zina zofanana ndi izo. Woyamba uja ndi shirk chifukwa Satana satumikira mfiti pokhapokha atakanira Allah. Tsono mtundu wachiwiriwo ndi tchimo lomuika munthu mu chiononongeko ndiponso mu machimo akuluakulu. Zonsezi zimachitika malinga ndi chikonzero cha Allah.

# DU'AA (PEMPHERO)

Zolengedwa zonse n'zosaukira kwa Allah zimasowa zomwe zili kwa Iye (SW), ndipo Iye Ngwachikwanekwane sawasowa iwo. Ndipo Allah anakhazikitsa Duaa pa akapolo Ake, ndipo anati "*Ndipempheni ndikuyankhani, ndithu amene amadzitukumula osandipempha adzakalowa ku Jahannam ali onyozeka*", nayenso Mtumiki (SAW) anati "*Amene samupempha Allah, Allah amamkwiyira iye*".**(Ibn Maajah).** Kuonjezera apa Allah amasangalala ndikupempha kwa akapolo Ake pakum'pempha Iye, ndipo amawakonda okakamira kuchita Du'aa kufunitsitsa kuti ayankhidwe ndipo amawayandikitsa kwa Iye.

Ndipo Maswahaaba a Mneneri (SAW) anazimvetsetsa zimenezi, ndipo sadali mmodzi wa iwo akunyozera kalikonse kuti kameneko ampemphe Allah, ndipo sanali kuwapereka mapempho awo kwa aliyense mu zolengedwa za Allah, ndipo zimenezo sizinali kuchitika wamba koma chifukwa cha mgwirizano wawo ndi Mbuye wawo, ndi kuyandikira kwawo kwa Iye (SW), komanso kuyandikira Kwake (SW) ndi iwo, pofuna kukwaniritsa mau Ake (SW) onena kuti "*Ndipo akapolo Anga akakufunsa za Ine ndithu Ine ndili pafupi*". Ndipo Duaa ili ndi gawo lalikulu pa maso pa Allah, choncho Duaayo ndi chinthu cholemekezeka pamaso pa Allah, ndipo nthawi zina imatha kubweza chigamulo cha Allah. Ndipo pempho la Msilamu limayankhidwa ngati patapezeka zifukwa ndikuchoka zoletsa, ndipo wopemphayo amapatsidwa chimodzi mwa zinthu zomwe Mneneri (SAW) wazitchula ndi mau ake onena kuti "*Palibe Msilamu amene angapemphe Duaa iliyonse yopanda mkati mwake tchimo, kapena kudula ubale, koma Allah amampatsa iye ndi Duaa imeneyo chimodzi mwa zinthu zitatu: Mwina kum'patsa iye chopempha chake mwamsanga, kapena kumusungira chimene wapemphacho kuti akachipeze ku Aakhirat, ndiponso mwina kumuchotsera vuto lofanana ndi pempho lakelo. Maswahaaba anati*" Ngati zili choncho ndiye kuti tichulutsa kuchita Duaa." Mtumiki (SAW) anati "*Allah ndi Wochulutsa kwambiri*". **(Ahmad).**

**MITUNDU YA DU'AA: Iyi ili pawiri:**

**1) Duaa ya ibaadat:** monga Swalaat ndi swaum. 2) Duaa ya kupempha ndi kufuna.

**KUSIYANA KWA NTCHITO (ZABWINO):** Kodi kuwerenga Qur'an n'kopambana, kapena Zikr, kapena Duaa, kapena kufuna? Kuwerenga Qur'an ndi ntchito yopambana kwambiri mosayerekeza ndi chilichonse, kenako zikr ndi kutamanda, kenako Duaa ndi kufuna, ndipo zimenezi zanenedwa mwachidule, koma nthawi zina chopambanidwacho chimatha kupezedwa ndi chinthu chomwe chingapangitse chinthucho kukhala chopambana kuposa chomwe chinali chopambana, choncho kuchita Duaa tsiku la Arafat n'kopambana kusiyana ndi kuwerenga Qur'an, komanso kutanganidwa ndi ma zikr omwe anadza pambuyo pa Swalaat za fardh ndibwino kwambiri kusiyana ndi kuwerenga Qur'an.

**ZIFUKWA ZOPANGITSA KULANDIRIDWA DUAA**

**Pali zifukwa zoonekera ndi zosaonekera:**

(1) Zifukwa zoonekera ndi: Kutsogoza ntchito zabwino: monga sadaka ndi wudhu, kuswali, kulunjika ku Qiblat, kutukula manja awiri,ndi kum'tamanda Allah ndi zomuyenerera Zake komanso kugwiritsa ntchito maina a Allah ndi mbiri Zake zolingana ndi opemphedwa. Choncho ikakhala Duaa yopempha Jannat kudzakhala

kudzichepetsa potchula ubwino Wake (SW) ndi chisomo Chake. Ndipo akapemphedwa kuti alangidwe wopondereza mwachitsanzo, ndiye kuti asatumikire dzina loti AIRAhmaan (Wachisoni chambiri), kapena dzina loti Alkareem (Woolowa manja), koma ligwiritsidwe ntchito dzina loti AlJabbaar (Wamphamvu), kapena loti AlQah-haar (Waukali). Ndipo zina mwa zifukwazo ndi izi: Kunena swaliyatume kumayambiriro kwa Duaayo, pakati pake ndi kumapeto kwake, kuvomereza machimo omwe munthu ali nawo, kumuthokoza Allah pa mtendere Wake, kupezerapo mwayi mu nthawi zopambana zomwe umboni wadza kuti nthawi zimenezo zikuganiziridwa kuyankhidwa Duaa, zina mwa izo ndi izi:

**MU USANA NDI USIKU:** Gawo lomaliza mwa magawo atatu a usiku pamene Allah amatsika mpaka pa mtambo wa dziko lapansi, pambuyo pa Azaan ndi Iqaamat, pambuyo pa wudhu, pa sajdat, asanapereke salaam ya Swalaat, pambuyo pa Swalaat zosiyanasiyana, pomaliza kuwerenga Qur'an yonse, tambala akamalira, paulendo, pempho la munthu woponderezedwa ndi wosimidwa, Duaa ya kholo kwa mwana wake, Duaa ya Msilamu kwa m'bale wake mwamseli, pokumana ndi adani pa nkhondo.

**MKATI MWA SABATA**:

Tsiku la Jumuat: Kwenikweni kamphindi komaliza ka tsikulo.

**M'MIYEZI**

Mwezi wa Ramadhaan pomasula ndi podya daku, usiku wa Lailatulqadr ndi tsiku la Arafat.

**M'MALO OLEMEKEZEKA:** M'mizikiti yonse, pa Ka'bat makamaka pa Multazam (pakati pa mwala wakuda ndi khomo la Ka'bat), pa Maqaam Ibrahim (AS), pamwamba pa Swafa ndi Marwat, pa Arafaat ndi Muzdalifat komanso Mina m'masiku a Hajj, pakumwa madzi a Zamzam ndi zina zotero.

(2) Zifukwa zobisika: Asanayambe Duaa ayenera kutsogoza Toba ya choonadi, kubweza zoponderezedwa, zakudya, zakumwa, zovala ndi malo okhala zikhale zochokera mu ntchito ya Halaal, kuchulutsa kuchita zabwino, kupewa za Haraam, komanso kudzisunga ku zokaikitsa ndi zilakolako. Ndipo mkatikati mwa Duaa mtima ukhale uli pompo, kukhala ndi chikhulupiriro mwa Allah, akhale ndi chiyembekezo champhamvu, papezeke kuthawira kwa Iye (SW), kukhudzumuka, kukakamira, chilichonse chochitika kuchipereka m'manja mwa Iye (SW), kusiya kuganiza chilichonse chosakhala Iye (SW), ndi kukhala ndi chitsimikizo choti ayankhidwa.

**ZOLEPHERETSA KUYANKHIDWA DUAA:**

Nthawi zina munthu amatha kupempha koma osayankhidwa, kapena amayankhidwa mochedwa. Ndipo zifukwa zake zilipo zambiri, zina mwa izo ndi izi:

✸Kuchipempha chosakhala Allah pamodzi ndi Allah. ✸ Kulongosola kwambiri pochita Duaa; monga kudzitchinjiriza ku kutentha kwa Jahannam, kupanikizika kwake komanso mdima wake ndi zina zotero chikhalirecho zikukwanira kungodzitchinjiriza ku moto basi. ✸ Kuchita Duaa yodzitemberera, kapena kum'temberera wina mopondereza. ✸ Kupempha za uchimo ndi zodula ubale. ✸ Kuchita Duaa molumikiza ndi mau oti ngati mungafune; monga kunena kuti E, Allah! Ndikhululukireni ngati mungafune ndi ma Duaa ena otero. ✸

Kufulumizitsa kuyankhidwa Duaa kufika ponena kuti: ndapempha ndipo sindinayankhidwe. ✸ **Kutaya mtima:** Komwe ndi kusiya kuchita Duaa chifukwa cha kutopa ndi kupempha. ✸ Kuchita Duaa ndi mtima wosalabadira wa masewera. ✸Kusowa ulemu pamaso pa Allah. Tsiku lina Mtumiki (SAW) anamumva munthu akupempha mu Swalaat yake koma sananene swaliyatume, ndipo Mneneri (SAW) anati "Munthuyo wafulumira", kenako anamuitana ndipo ananena kwa iye kapena kwa wina wake kuti: "*Mmodzi wa inu akafuna kuchita Duaa ayambe ndi kum'tamanda Allah ndi kumuyamikira, kenako anene swaliyatume ndipo pambuyo pake apemphe zomwe akufuna*" **(Tirmidhi).** ✸ Kupempha zinthu zoti wathana nazo; monga kupempha kuti adzakhale mpaka kalekale pa dziko lapansi. ✸ Kusanja kodzikakamiza pochita Duaa, Allah akunena kuti "*Mpempheni Mbuye wanu modzichepetsa komanso mwachinsinsi, ndithu Iye sawakonda anthu opyola malire*" **(Surat 7:55),** ndipo Ibn Abbas (RA) ananena kuti "Uziona kusanja kwa Duaa ndipo udzikupewa, pakuti ine ndinamuona Mtumiki wa Allah (SAW) ndi Maswahaaba ake sanali kusanja koma anali kukupewa kusanjako" **(Bukhaari).** ✸ Kupitirira muyezo pokweza mau pa Duaa. Allah ananena kuti: "Ndipo usakweze mau kwambiri pochita Duaa yako komanso usanong'one kwambiri pochita Duaayo, koma tsata njira yolingana pakati pa zimenezo" (Surat 17:110).
Bibi Aisha (RA) anati Ayat imeneyi inavumbulutsidwa pa nkhani ya Duaa.
Ndibwino kuti wochita Duaa asanje Duaa yake motere: Poyambirira amutamande Allah ndi kumuyamikira ponena kuti: Alhamdu lillaahi Kachiwiri kunena swaliyatume ponena kuti: ALLAHUMMA SWALLI ALA MUHAMMAD, kapena kuti: WASSWALAATU WASSALAAMU Kachitatu kuchita Toba ndikuvomera tchimo lomwe ali nalo, Kachinayi kumuthokoza Allah pa mtendere Wake, Kachisanu kuyamba kuchita Duaa ndikuyesetsa kubweretsa Duaa yachikwanekwane, ndi yomwe inatsimikizika kuchokera kwa Mneneri (SAW), kapena kwa akuluakulu akale a chipembedzo, Chachisanu ndi chimodzi kumaliza Duaa ndi swaliyatume.

## MADUAA OFUNIKA OYENERA KUWASUNGA:

| ZOCHITIKA | DU'AA: MNENERI (SAW) ANATI: |
|---|---|
| POGONA NDI PODZUKA | « بِاسْمِكَ اللَّهُمَّ أَمُوتُ وَأَحْيَا »[1]<br>ndipo akadzuka anene kuti: « الْحَمْدُ لِلَّهِ الَّذِي أَحْيَانَا بَعْدَمَا أَمَاتَنَا وَإِلَيْهِ النُّشُورُ »[2] |
| AMENE AMADZIDZIMUKA KUTULO ANENE KUTI | « أَعُوذُ بِكَلِمَاتِ اللَّهِ التَّامَّاتِ مِنْ غَضَبِهِ وَعِقَابِهِ، وَمِنْ شَرِّ عِبَادِهِ، وَمِنْ هَمَزَاتِ الشَّيَاطِينِ، وَأَنْ يَحْضُرُونِ »[3] |
| WA MTULO AKALOTA | Mmodzi wa inu akalota maloto abwino ndiye kuti amenewo achokera kwa Allah (SW), choncho amtamande Allah chifukwa cha malotowo ndipo awanene kwa munthu wina, ndipo akalota zosakhala bwino ndiye kuti zachokera kwa Satana, choncho adzitchinjirize ku maloto oipawo ndipo asamuuze wina aliyense, pakutero malotowo sangampatse vuto. |

[1] "MDZINA LANU Ambuye ndikufa ndidzadzukanso"
[2] "Chitamando chonse ndi cha Allah Amene watipatsa moyo pambuyo poti anatipatsa imfa ndipo tidzaukitsidwa kupita kwa Iye".
[3] Ndikudzitchinjiriza ndi mau a Allah okwanira ku ukali Wake, ku zoipa za akapolo Ake, kumipungwepungwe ya asatana, ndikutinso andifikire.

| | |
|---|---|
| **POTULUKA M'NYUMBA** | [1] « اللّهمّ إني أعوذ بك أن أضل أو أضل، أو أزل أو أزل، أو أظلم أو أظلم، أو أجهل أو يجهل علي »<br>[2] « بسم الله توكلت على الله لا حول ولا قوة إلا بالله » |
| **POLOWA MU MZIKITI** | Akafuna kulowa mu Mzikiti atsogoze mwendo wake wamanja ndipo anene kuti: بِسْمِ اللّه وَالسَّلامُ عَلَى رَسُولِ اللَّه اللَّهُمَّ اغْفِرْ لِى ذُنُوبِى وَافْتَحْ لِى أَبْوَابَ رَحْمَتِكَ[3] |
| **POTULUKA MU MZIKITI** | Akamatuluka mu Mzikiti atsogoze mwendo wake wamanzere ndipo anene kuti: بِسْمِ اللّه وَالسَّلامُ عَلَى رَسُولِ اللَّه اللَّهُمَّ اغْفِرْ لِى ذُنُوبِى وَافْتَحْ لِى أَبْوَابَ فَضْلِكَ[4] |
| **AMENE WANGOKWATIRA KUMENE NENANI KWA IYE KUTI** | [5] « بارك الله لك، وبارك عليك، وجمع بينكما في خير » |
| **AMENE WAMVA KULIRA KWA TAMBALA KAPENA BULU** | Mtumiki (SAW) anati "Mukamva kulira kwa bulu; dzitchinjirizeni mwa Allah ku Satana pakuti iyo yaona Satana, ndipo mukamva kulira kwa tambala; mpempheni Allah mtendere Wake pakuti iyo yaona Mngero", Mukamva kuuwa kwa galu, kapena kulira kwa bulu nthawi ya usiku dzitchinjirizeni mwa Allah. |
| **UKADZIWITSIDWA KUTI WINA WAKE AKUKUKONDA MWA ALLAH** | Hadith inachokera kwa Anas (RA) kuti munthu wina anali kwa Mneneri (SAW) tero munthu wina anadutsa, ndipo munthu uja anati: "E, inu Mtumiki wa Allah! Ndithu ine ndimaamkonda uyu. "Choncho Mneneri (SAW) anati kwa iye". Unamudziwitsa kuti umamkonda?" Munthu uja anati, Mtumiki (SAW) anati "Umudziwitse". Choncho anapita pomwe panali iye namuuza kuti ine ndimakukonda iwe chifukwa cha Allah, anati akukonde iwe amene wakupangitsa kuti undikonde chifukwa cha Iye. |
| **M'BALE WANU WACHISILAMU AKAYATSAMULA** | Mmodzi wa inu akayatsamula ayenera kunena kuti "***Alhamdulillah***", ndipo m'bale wake kapena mnzake ayenera kunena kwa iye kuti "***YarhamukAllah***", (Allah akuchitire chisoni), choncho akanena kwa iye kuti yarhamukAllah (Allah akuchitire chisoni) ayenera kunena kuti "***Yah dee kumullahu wayus-lih baalakum***" (Allah akuongolereni ndi kukukonzerani zochita zanu). Ndipo kafiri akayatsamula namtamanda Allah nena kwa iye kuti, ***Yah dee kumullah*** (Allah akuongoleni) ndipo musanene kuti, ***YarhamukAllah*** (Allah akuchitireni chisoni). |
| **DUWA YA PAMAVUTO** | « لا إله إلا الله العظيم الحليم، لا إله إلا الله رب العرش العظيم، لا إله إلا الله رب السموات ورب الأرض ورب العرش الكريم »[6] ✸ « سبحان الله العظيم »[7] ✸<br>[1] « ياحي يا قيوم برحمتك أستغيث » ✸ « اللّه اللّه ربي، لا أشرك به شيئا »[8] ✸ |

[1] "E, Mbuye wanga! Ine ndikudzitchinjiriza kwa Inu kuti ndimusocheretse wina kapena kuti ndisocheretsedwe, kapena kuti ndimulakwitse wina kapena kuti ndilakwitsidwe, kapena kuti ndipondereze kapena ndiponderezedwe, kapena kuti ndimchitire za umbuli wina kapena kuchitiridwa za umbuli".

[2] "Mdzina la Allah ndayedzamira mwa Allah palibe nzeru yosiyira zoipa kapena mphamvu yochitira zabwino koma zonse zili m'manja mwa Allah".

[3] "Mdzina la Allah mtendere upite kwa Mtumiki wa Allah E, Mbuye wanga! Ndikhululukireni ine machimo anga ndipo nditsegulireni makomo a chisoni Chanu"

[4] "Mdzina la Allah mtendere upite kwa Mtumiki wa Allah E, Mbuye wanga! Ndikhululukireni ine machimo anga ndipo munditsegulire makomo a mtendere Wanu".

[5] "Allah akupatse madalitso iwe ndi zochita zako, ndipo asonkhanitse pakati pa awirinu mtendere".

[6] Palibe wopembedzedwa mwachoonadi kupatula Allah ,Wamkulu,Wodekha, Palibe wopembedzedwa mwachoonadi kupatula Allah Mbuye wa mpando waukulu wachifumu. Palibe wopembedzedwa mwachoonadi kupatula Allah Mbuye wa mitambo komanso Mbuye wa nthaka ndinso Mbuye wa mpando wachifumu waulemerero.

[7] Wayera Allah, Wamkulu kwambiri.

[8] Allah,Allah Mbuye wanga, ine sindikum'phatikiza limodzi ndi Iye kanthu kena kalikonse.

| | |
|---|---|
| PAKAPEZEKA VUTO | «لا إله إلا الله وحده لا شريك له، له الملك وله الحمد وهو علي كل شيء قدير، الحمد لله وسبحان الله ولا إله إلا الله والله أكبر ولا حول ولا قوة إلا بالله» [2] |
| KUWATEMBERERA ADANI | «اللهم منزل الكتاب ومجري السحاب سريع الحساب اهزم الأحزاب، اللهم اهزمهم وزلزلهم» [3] |
| CHINA CHAKE CHIKAVUTA | [4] «اللهم لا سهل إلا ما جعلته سهلا وأنت تجعل الحزن إذا شئت سهلاً» |
| DU'AA YOBWEZERA NGONGOLE | «اللهم إنى أعوذ بك من الهم والحزن والعجز والكسل والجبن والبخل، وضلع الدين، وغلبة الرجال» [5] |
| KU CHIMBUDZI | Polowa m'chimbudzi anene kuti: [6] «اللهم إني أعوذ بك من الخبث والخبائث» ndipo potulukamo anene kuti, غفرانك "ndikupempha chikhululuko Chanu". |
| MANONG'ONONG'O A PA SWALAAT | Amene uja ndi Satana amatchedwa kuti Khanzab, choncho ukamuzindikira udzitchinjirize mwa Allah kwa iye ndipo ulavulire kumanzere katatu). |
| PA SAJDAT | [8] «سبحانك ربي وبحمدك اللهم اغفر لي» ✹ [7] «اللهم اغفر لي ذنبي كله دقه وجله وأوله وآخره وعلانيته وسره» [9] «اللهم إني أعوذ برضاك من سخطك وبمعافاتك من عقوبتك وأعوذ بك منك لا أحصى ثناء عليك أنت كما أثنيت على نفسك» ✹ |
| PA SAJDAT YA TILAWAT | [10] «اللهم لك سجدت وبك آمنت ولك أسلمت سجد وجهي للذي خلقه وصوره وشق سمعه وبصره تبارك الله أحسن الخالقين» |
| KUMAPETO KWA SWALAAT | [11] «اللهم إني ظلمت نفسي ظلما كثيرا ولا يغفر الذنوب إلا أنت فاغفر لي مغفرة من عندك وارحمني إنك أنت الغفور الرحيم» |
| KUTHA KWA SWALAAT | [13] «اللهم إني أعوذ بك من الكفر والفقر وعذاب القبر» ✹ [12] «اللهم أعني على ذكرك وشكرك وحسن عبادتك» ✹ |

---

[1] Eh inu Amoyo komanso Muimiriri wa chinthu chili chonse! Kudzera mu chisoni chanu ine ndikudzitchinjiriza.

[2] Palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma Allah Wolemekezeka Woleza mtima, palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma Allah Mwini mpando wachifumu wolemekezeka, palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma Allah Mwini kumwamba ndi pansi komanso Mwini mpando wachifumu wolemekezeka, Allah, Allah ndiye Mbuye wanga, sindikuphatikizani ndi kena kake, (E, Inu Wamoyo, Inu M'yang'aniri kudzera mu chisoni Chanu ndikupempha chipulumutso. Chiyero ndicha Allah Wolemekezeka).

[3] "E, Mbuye wanga Amene mumayendetsa mitambo, Amene munavumbulutsa Qur'an. Amene m'mawerengera mwachangu! Agonjetseni magulu a adani, E, Mbuye wanga aonjetseni ndi kuwagwedeza".

[4] "E, Allah! palibe chosavuta kupatula chimene mwachichita kukhala chosavuta, ndipo Inu mumawachita madandaulo mukafuna kukhala osavuta".

[5] "E, Mbuye wanga! Ine ndikudzitchinjiriza mwa Inu ku maganizo ndi madandaulo, kulephera ndi ulesi, mantha ndi umbombo, kulemedwa ndi ngongole ndi kugonjetsedwa ndi anthu".

[6] "E, Mbuye wanga! Ine ndikudzitchinjiriza mwa Inu ku ziwanda zoipa zazimuna ndi zazikazi"

[7] "E, Mbuye wanga! Ndikhululukireni ine machimo anga onse aang'onoang'ono ake ndi aakuluakulu ake, oyambirira ndi omalizira ake, owachita moonekera ndi mwachinsinsi".

[8] "Mbuye wanga kuyera ndi kutamandidwa ndi Kwanu, ndikhululukireni Mbuye wanga".

[9] "E, Mbuye wanga! Ine ndikudzitchinjiriza ndi chiyanjo Chanu ku ukali Wanu, kukhululuka Kwanu ku chilango Chanu, komanso ndikudzitchinjiriza mwa Inu ku chilango chochokera kwa Inu, sindingakwanitse kukutamandani monga momwe mwadzitamandira".

[10] "E, Mbuye wanga! Ndakulambirani, mwa Inu ndakhulupirira, ndiponso ndadzipereka kwa Inu, nkhope yanga yalambira kwa amene anailenga, anaipatsa chithunzi chabwino, anaiboolera makutu ndi kuipatsa maso, Allah ndi Mwini madalitso ochuluka, Wolenga bwino kuposa olenga onse".

[11] "E, Allah! Ine ndadzipondereza kwambiri ndipo palibe wokhululuka machimo kupatula Inu, choncho ndikhululukireni ndi chikhululuko chochokera kwa Inu, ndipo ndichitireni chisoni pakuti Inu Ndinu Wokhululuka Achifundo".

[12] E, Mbuye wanga! Ndithandizeni kuti ndikhale wokukumbukirani ndi kukuthokozani komanso wolongosola ibaadat Yanu.

[13] E, Allah! Ine ndikudzitchinjiriza mwa Inu ku ukafiri, umphawi ndi ku chilango cha manda.

| | |
|---|---|
| **AMENE WACHITIRIDWA ZABWINO** | Amene wachitiridwa zabwino nanena kwa amene wachita zabwinoyo kuti JazakAllahu khairan (Allah akulipireni zabwino) ndiye kuti wayamika kwambiri, winayonso abwezere ndi mau ake onena kuti inunso akulipireni zabwino. |
| **AKAIONA MVULA** | Anene kawiri kapena katatu kuti ✷ « اللّهمّ صَيِّبًا نَافعًا » "**ALLAHUM'MA SWAIYIBAN NAAFI-AN**"[1] anenenso kuti: tapatsidwa mvula mchisomo cha Allah ndi chifundo Chake, ndipo apemphe kwa Allah chimene akufuna, pakuti Du'aa imayankhidwa pamene mvula ikuvumba. « مُطِرْنَا بِفَضْلِ اللهِ وَرَحْمَتِهِ » ✷ |
| **IKAMAOMBA MPHEPO YA MKUNTHO** | [2] « اللّهمّ إني أسألك خَيْرَهَا وخيرَ مَا فيهَا وخيرَ ما أرسلت به وأعوذُ بكَ مِنْ شَرِّهَا وَشَرِّ مَا فيهَا وشَرِّ ما أُرسلت به » |
| **AKACHIONA CHITHUNZI CHA MWEZI CHATSOPANO** | [3] « اللهمّ أَهِلَّه عَلَيْنَا بِاليمن والإيمَان والسَّلامَة وَالإسْلام هلالِ خَيْرٍ وَرُشْد، ربي وربُّك اللهُ » |
| **AMENE AKUTSAZIKANA NDI WAPAULENDO** | [4] « أَسْتَوْدِعُ اللَّهَ دِينَكَ وَأَمَانَتَكَ وَخَوَاتِيمَ عَمَلِكَ » **ndipo wapaulendo am'bwezere iye ponena kuti:** [5] « أَسْتَوْدِعُكُمُ اللهَ الَّذِي لا تَضِيعُ وَدَائِعُهُ » |
| **UKAONA CHOMWE UKUCHIKONDA KAPENA CHIMENE UKUCHIDA** | **Mtumiki (SAW) ankati akaona chimene akuchikonda ankanena kuti:** [6] « الحَمْدُ لِله الَّذِي بِنِعْمَتِهِ تَتِمُّ الصَّالحاتُ » **Ndipo akaona chimene akudana nacho ankati:** [7] « الحَمْدُ لله على كلِّ حال » |
| **DU'AA YA PAULENDO** | اللهُ أَكْبَر، اللهُ أَكْبَر، اللهُ أَكْبَر ﴿ سُبْحَانَ الَّذِي سَخَّرَ لَنَا هَذَا وَمَا كُنَّا لَهُ مُقْرِنِينَ ✷ وَإِنَّا إِلَى رَبِّنَا لَمُنقَلِبُونَ ﴾ اللَّهُمَّ إِنَّا نَسْأَلُكَ فِي سَفَرِنَا هَذَا الْبِرَّ وَالتَّقْوَى، وَمِنَ الْعَمَلِ مَا تَرْضَى، اللَّهُمَّ هَوِّنْ عَلَيْنَا سَفَرَنَا هَذَا وَاطْوِ عَنَّا بُعْدَهُ، اللَّهُمَّ أَنْتَ الصَّاحِبُ فِي السَّفَرِ وَالْخَلِيفَةُ فِي الأَهْلِ اللَّهُمَّ إِنِّي أَعُوذُ بِكَ مِنْ وَعْثَاءِ السَّفَرِ وَكَآبَةِ الْمَنْظَرِ وَسُوءِ الْمُنْقَلَبِ فِي الْمَالِ وَالأَهْلِ. **Ndipo akamabwerera anene Du'aa imeneyi ndikuonjezera mau oti:**[8] آيِبُونَ تَائِبُونَ عَابِدُونَ لِرَبِّنَا حَامِدُونَ[9] |

[1] (E, Allah! Tipatseni mvula yopindulitsa),
[2] E, Allah! Ine ndikukupemphani zabwino za mphepoyo, zabwino zili m'menemo, ndi zabwino zomwe yatumizidwa nazo, ndipo ndikudzitchinjiriza mwa Inu ku zoipa zake, zoipa zili m'menemo ndi zoipa zomwe yatumizidwa nayo.
[3] "E, Allah! Chionetseni chithunzicho kwa ife ndi madalitso, Imaan, mtendere ndi kugonjera, chikhale chithunzi cha mwezi cha mtendere ndi chiongoko, Mbuye wanga komanso Mbuye wako ndi Allah".
[4] "Ndikum'pempha Allah kuti akusungire Deen yako, kukhulupirika kwako ndi komalizira kwa ntchito yako",
[5] "Ndikum'pempha Allah kuti akusungeni, Amene zosunga Zake sizimasokonekera".
[6] "Kutamandika konse ndi kwa Allah amene kudzera mu mtendere wake zabwino zonse zimakwaniritsika."
[7] "Kutamandika konse ndi kwa Allah m'mene zinthu zingakhalire".
[8] "Allah ndi Wamkulu koposa, Allah ndi Wamkulu koposa, Allah ndi Wamkulu koposa" chiyero ndicha Amene Watifewetsera chokwerachi ndipo tinalibe kuthekera kochiongolera. Ndipo ndithudi ife tidzabwerera kwa Mbuye wathu. E, Allah! Ife tipempha Inu mu ulendo wathuwu zabwino, zoopa Inu ndi ntchito yomwe Mungaiyanje, E, Allah! Tipeputsireni ulendo wathuwu ndi kutifupikitsira mtunda wake, E, Allah! Ndinu Wotsagana Nanu paulendo, komanso Woyang'anira panyumba panga, E, Allah! Ine ndikudzitchinjiriza mwa Inu ku zoipa zapaulendo, maonekedwe oipa ndikuti ndibwerere mosakhala bwino ku chuma changa ndi banja langa".
[9] "Tikubwerera tikupanga toba, tikupanga ibaadat, tikum'tamanda Mbuye wathu".

| | |
|---|---|
| POGONA | [1] ✷ « اللهم أسلمت نفسى إليك وفوضت أمري إليك وألجأت ظهري إليك رهبة ورغبة إليك لا ملجأ ولا منجا منك إلا إليك آمنت بكتابك الذي أنزلت وبنبيك الذي أرسلت »<br>[2] « الحمد لله الذي أطعمنا وسقانا وكفانا وآوانا فكم ممن لا كافي له ولا مؤوي » ✷<br>[3] « اللهم قني عذابك يوم تبعث عبادك » ✷<br>[4] ✷ « سبحانك اللهم ربى بك وضعت جنبى وبك أرفعه إن أمسكت نفسى فاغفر لها وإن أرسلتها فاحفظها بما تحفظ به عبادك الصالحين »<br>✷ Auzire m'manja ake awiri ndipo awerenge surat Nas ndi Falaq ndikusisita ndi manja awiriwo thupi lake asagone usiku wonse mpaka atawerenga Alif Laam Sajdat, komanso surat Mulk. |
| KUTSEGULIRA SWALAAT | [5] « اللهم باعد بيني وبين خطاياي كما باعدت بين المشرق والمغرب، اللهم نقني من خطاياي كما ينقى الثوب الأبيض من الدنس، اللهم اغسلنى بالماء والثلج والبرد » |
| POPITA KOKASWALI | [6] « اللهم اجعل في قلبي نورا وفي لساني نورا وفي سمعي نورا وفي بصري نورا ومن فوقي نورا ومن تحتي نورا وعن يميني نورا وعن شمالي نورا ومن أمامي نورا ومن خلفي نورا واجعل في نفسي نورا وأعظم لى نورا وعظم لى نورا واجعل لى نورا واجعلنى نورا اللهم أعطنى نورا واجعل فى عصبى نورا ، وفى لحمى نورا ، وفى دمى نورا ، وفى شعري نورا ، وفى بشري نورا » |
| DU'AA YA ISTIKHARAH (Yopempha zabwino) | **Mmodzi wa inu akatsimikiza kuchita chinthu aswali marakaat awiri osakhala a Faradh ndipo akamaliza anene kuti:**[7]<br>« اللهم إني أستخيرك بعلمك، وأستقدرك بقدرتك، وأسألك من فضلك فإنك تقدر ولا أقدر وتعلم ولا أعلم وأنت علام الغيوب، اللهم فإن كنت تعلم هذا الأمر ( ثم تسميه بعينه ) خيرا لي في ديني ومعاشي وعاقبة أمري . أو قال: عاجل أمري وآجله . فاقدره لي ويسره لي ثم بارك لي فيه وإن كنت تعلم أن هذا الأمر شر لي في ديني ومعاشي وعاقبة أمري. أو قال في عاجل أمري وآجله . فاصرفه عني واصرفني عنه |

[1] "E, Allah! Ndaupereka moyo wanga kwa Inu, ndiponso ndazipereka zochitika zanga kwa Inu, ndi kuwuthawitsira msana wanga kwa Inu, mwa mantha ndi chiyembekezo kwa Inu, palibe kothawira ndi kupulumukira ku chilango Chanu koma kwa Inu, ndalikhulupirira Buku Lanu lomwe munalivumbulutsa, komanso Mneneri Wanu amene munamtuma".

[2] "Kutamandika konse ndi kwa Allah Amene watipatsa chakudya ndi chakumwa ndipo watikwaniritsa komanso watipatsa malo ogona, ndi angati amene alibe wowakwaniritsa ngakhale kuwapatsa malo ogona".

[3] "E, Allah! Mukandipulumutse ku chilango Chanu pa tsiku limene Mudzaukitse akapolo Anu".

[4] "Kuyera ndi Kwanu E, Mbuye wanga! Mbuye wanga! Kudzera mwa Inu ndagoneka nthiti yanga kugona ndipo ndidzaidzutsa kudzera mwa Inu mukachotsa moyo wanga, choncho ukhululukireni moyowo, ndipo ngati mutaumasula uyang'anireni ndi zomwe mumawayang' anira akapolo Anu ochita zabwino".

[5] "E, Allah! Talikitsani pakati pa ine ndi machimo anga monga momwe munachitira Kuvuma ndi Kuzambwe, E, Allah! Ndiyeretseni ku machimo anga monga momwe imayeretsedwera nsalu yoyera ku litsiro, E, Allah! Ndisambitseni ndi madzi, ayesi komanso mame.

[6] "E, Allah! Ikani mumtima mwanga, pa lirime langa, m'makutu mwanga, m'maso mwanga, pamwamba panga, kupansi kwanga, chakumanja kwanga, chakumanzere kwanga, patsogolo panga ndi kumbuyo kwanga kuwala, ndiponso ikani mumtima mwanga kuwala, komanso mundikulitsire kuwala, ndikundilemekezera kuwala, ndipatseni kuwala, ndikundichita ine kukhala kuwala, E, Allah! Ndipatseni kuwala, ikani m'mitsempha yanga, mnyama yanga, m'magazi anga, mutsitsi langa, komanso mu khungu langa kuwala".

[7] "E, Allah! Ine ndikukupemphani zabwino kudzera mu kuzindikira Kwanu, ndikukupemphani kuthekera kudzera mu mphamvu Yanu, ndikupempha chisomo Chanu, pakuti Inu muli ndi kuthekera pomwe ine ndilibe kuthekera ndipo Inu mumadziwa pomwe ine sindidziwa, ndipo Inu mumadziwa kwambiri zanseli, E, Allah! Choncho ngati Inu mukudziwa kuti chinthu ichi (kenako pamenepa achitchule chinthucho) ndi chabwino kwa ine mu Deen yanga, m'moyo wanga, komanso kumapeto kwa zochita zanga. Kapena anene kuti "Panopa kapena mtsogolo – choncho ndipatseni kuthekera kwake ndipo ndipeputsireni ndikundiyikiramo madalitso, ndipo ngati mukudziwa kuti chinthuchi ndi choipa kwa ine mu Deen yanga, m'moyo wanga ndi m'mapeto a zochita zanga, kapena anene kuti n'zochita zanga zapanopo kapena za mtsogolo – choncho chipewetseni kwa ine, ndikundipewetsa ine ku icho, ndipo ndipatseni kuthekera kopeza chabwino kulikonse kumene chili, kenako mundichite kukhala wochiyanja chinthucho".

| | |
|---|---|
| | وَاقْدُرْ لِى الْخَيْرَ حَيْثُ كَانَ ثُمَّ رَضِّنى بِه |
| **YA MALIRO** | .......اللهم اغفر له وارحمه وعافه واعف عنه وأكرم نزله ووسع مدخله<br>Oh Allah, mukhululukireni, m'chitireni chifundo, mpatseni moyo wabwino komanso mufafanizireni machismo ake. Lemekezani malo wofikira iye, m'tambasulireni malo mwake alowemo. Msambitseni ndi madzi, ayezi ndi matalala ndipo muyeretseni kumachimo mumayeretsera nsalu yoyera ku uve. Msinthireni nyumba yabwino yoposa nyumba yake, abale ake abwino kuposa amene anali nawo, mkazi wabwino kuposa mkazi wake ndipo mulowetseni ku Jannat ndikumutchinjiriza ku chilango cha moto. |
| **KUCHOTSA MADANDAULO** | **Palibe akiyense angampeze maganizo mu mtima mwake kapena madandaulo ndipo iye nati:**<br>« اللَّهُمَّ إِنِّي عَبْدُكَ وَابْنُ عَبْدِكَ وَابْنُ أَمَتِكَ نَاصِيَتِي بِيَدِكَ مَاضٍ فِيَّ حُكْمُكَ عَدْلٌ فِيَّ قَضَاؤُكَ أَسْأَلُكَ بِكُلِّ اسْمٍ هُوَ لَكَ سَمَّيْتَ بِهِ نَفْسَكَ أَوْ عَلَّمْتَهُ أَحَدًا مِنْ خَلْقِكَ أَوْ أَنْزَلْتَهُ فِي كِتَابِكَ أَوِ اسْتَأْثَرْتَ بِهِ فِي عِلْمِ الْغَيْبِ عِنْدَكَ أَنْ تَجْعَلَ الْقُرْآنَ رَبِيعَ قَلْبِي وَنُورَ صَدْرِي وَجِلَاءَ حُزْنِي وَذَهَابَ هَمِّي »<br>Pokhapokha Allah amamuchotsera madandaulo akewo ndikumusinthira mmalo mwake chisangalalo.[1] |

[1] "Oh Allah! Ndithudi ine ndine kapolo wanu ndiponso mwana wakapolo wanu wachimuna komanso kapolo wanu wachikazi. Liwombo langa lili m'dzanja mwanu. Lamulo Lanu lichitika mwa ine. Chiweruzo chanu pa ine ndi chachilungamo. Ndikukupemphani kudzera m'dzina lili lonse lomwe ndi Lanu mwadzitcha nalo Nokha kapena mwamphunzitsa wina aliyense mu zolengedwa zanu kapena munalivumbulutsa mu Bukhu Lanu kapena mwadzisankhira Nokha ndi limenelo mukuzindikira za mseri komwe muli nako, ndikupemphani kuti muichite Quran kukhala chinyontho cha mtima wanga komanso dangalira la chidali change ndichochotsera madandaulo anga koma chochotsera maganizo."

# MALONDA APHINDU

Ndithu Allah anam'pambanitsa munthu pa zolengedwa zonse ndipo anamusankhira mtendere wa kuyankhula, ndipo anachichita chida chake kukhala lirime, ndipo lirimelo ndi mtendere womwe umagwiritsidwa ntchito pa zabwino kapena pa zoipa, ndipo amene angaligwiritsire ntchito pa zabwino limufikitsa ku chisangalalo cha padziko lapansi ndi ku maulemerero apamwamba aku Jannat, ndipo amene waligwiritsa ntchito posakhala pa zabwino likamufikitsa mzionongeko za mduniya ndiku Aakhirat. Ndipo chopambana chomwe nthawi ingapambane nacho pambuyo powerenga Qu'ran ndiye Zikrullah kumkumbukira Allah ndikumutchula.

## UBWINO WA ZIKRULLAH

Adza ma Hadith ochuluka onena za ubwino wake, ndipo ena mwa iwo ndi kuyankhula kwake (SAW) konena kuti: (Kodi ndikuuzeni ntchito yomwe ili yabwino mu ntchito zanu, yomwenso ili yoyera kwa Mfumu yanu, komanso yomwe ili yapamwamba mu ulemerero wanu, yabwino kwambiri kwa inu kuposa kupereka golide ndi siliva, ndiponso ndi zabwino kwa inu kuposa kuti mukakumane ndi adani anu n'kumadula makosi awo namakudulaninso makosi anu?" Maswahaaba anati "Inde inu Mtumiki wa Allah" Mtumiki (SAW) anati Ndi Zikrullah" **(Tirmidhi).** Ndikuyankhula kwake (SAW) konena kuti "*Fanizo la amene anamkumbukira Mbuye Wake ndi amene samkumbukira lili ngati wamoyo ndi wakufa*." **Kiyaamat(Bukhaari, Muslim)** . Ndinso kuyankhula kwa Allah (SW) mu Hadith Qudsi kunena kuti "*Ine ndili pafupi ndi maganizo a kapolo wanga amene akundiganiza Ine, ndiponso ndili naye limodzi akandikumbukira Ine, akandikumbuka mu mtima mwake ndimaamkumbukira mu mtima mwanga, ndipo akandikumbukira Ine mgulu ndidzamkumbukira mgulu labwino kuposa iwo, ndiponso akadziyandikitsa kwa Ine pamtunda wa mlingo wa chikhato ndidzadziyandikitsa kwa iye ndi mtunda wotalika ngati dzanja*" **(Bukhaari).** Ndi kuyankhula kwa Mtumiki (SAW) konena kuti: "*Atsogola ompatula Allah, Maswahaaba anafunsa kuti, E, Inu Mtumiki wa Allah kodi ompatula Allah ndi ndani?"* Mtumiki (SAW) anati "*Amuna ndi akazi omkumbukira Allah kwambiri*" **(Muslim),** komanso mau ake (SAW) pomulangiza mmodzi mwa Maswahaaba ake ponena kuti "*Nthawi zonse lirime lako lsasiye kukhala laliwisi chifukwa chomutchula Allah*" **(Tirmidhi, ndi ma Hadith ena).**

## KUONJEZEREKA MALIPIRO

Malipiro a ntchito zabwino amaonjezereka monga momwe amaonjezereka malipiro a kuwerenga Qur'an, ndipo zimenezi nchifukwa cha zinthu ziwiri izi:

1. Molingana ndi m'mene Imaan ilili mu mtima ndinso Ikhlas komanso kumkonda Allah kudzanso zotsatira zake.
2. Molingana ndi kulingalira kwa mtima ndi zikr, komanso ndi kutanganidwa kwake iye ndi zikriyo, choncho zikriyo isakhale ndi lirime lake basi. Motero ngati zakwanira zimenezo Allah amamufufutira machimo ake onse ndikum'patsa malipiro ake okwanira, ndipo kupunguka malipiro zili malinga ndi m'mene alili munthuyo.

## PHINDU LA ZIKR

Shaikhul Islaam (RA) ananena kuti zikr kumbali ya mtima ili ngati madzi kumbali ya nsomba, choncho ingaoneke bwanji nsomba ngati itasiyana ndi madzi?

✸ Kumapangitsa kuti Allah azim'konda iye, kuti azimuyandikira iye, kuti azimuyanja, kuti azimuyang'anira, kuti azimuopa, kuti adzithawira kwa Iye ndi kubwerera kwa Iye, komanso kumathandizira kumumvera Iye (SW). ✸ Kumachotsa maganizo ndi madandaulo mumtima ndikubweretsamo chisangalalo, ndiponso kumapangitsa mtima kukhala wamoyo, wamphamvu komanso woyera. ✸ Mumtima muli kuperewera ndi umphawi palibe chimene chingatseke zimenezo koma zikr ya Allah, mulinso kuuma moyo palibe chomwe chingasungunule kuumako kapena kufewetsa koma zikr ya Allah. ✸Zikrullah ndi machiritso a mtima, mankhwala ake, chakudya chake ndinso kukoma kwake komwe sikufanana ndi kukoma kwina kulikonse, ndipo kusalabadira posam'kumbukira Iye ndiye matenda ake. ✸ Kuchepa kwa kumkumbukira Allah ndi umboni wa uchiphamaso, ndipo kuchulutsa kuchita zikr ndi umboni wa kukhala ndi Imaan yamphamvu komanso kum'konda Allah m'choonadi, chifukwa amene wachikonda chinthu amachulutsa kuchitchula. ✸ Ndipo kapolo akadzizindikiritsa kwa Allah pomukumbukira Iye ali pamtendere Allah adzamudziwa iye ali pamavuto, kwenikweni pa nthawi yomwalira ndi ululu wake. ✸ Ndichifukwa chokapulumukira ku chilango cha Allah, kutsika mtendere wa Allah, kukutidwa ndi chisoni cha Allah, komanso kupemphereredwa makhululuko ndi angero. ✸ Lirime limatanganidwa ndi zikr n'kusiya zopanda pake, miseche, ukazitape, bodza, ndi zina zosakhala bwino komanso zoletsedwa. ✸ Zikr ndi imodzi mwa ibaadat yopepuka, yolemekezeka komanso yopambana, ndipo iyo ndi nkhalango yaku Jannat. ✸ Zikr imamveka wochita zikriyo ulemerero, kuzuna komanso kuwala pa nkhope, ndipo iyo ndi Noor pa dziko lino lapansi, m'manda, komanso ku bwalo la milandu. ✸ Zikr imapangitsa madalitso a Allah, ndi Du'aa ya Angero kuti zipite kwa munthu wochita zikr, ndipo Allah amawanyadira ochita zikr kwa Angero Ake. ✸ Opambana mwa anthu amene amachita ntchito zabwino ndi amene amachulutsa kum'kumbukira Allah, choncho opambana mwa anthu omwe amamanga swaum ndi amene amachulutsa kum'kumbukira Allah pamene akumanga swaum yake. ✸Zikr imafewetsa chovuta kukhala chosavuta, imapeputsa cholemera, imapeputsa mavuto, imabweretsa rizq komanso imalimbitsa thupi. ✸Zikr imapirikitsa Satana, imam'kwapula, komanso imamuyalutsa ndi kum'peputsa.

## MA DU'AA A M'MAWA NDI MADZULO PA TSIKU LILI LONSE

| N | MADU'AA APATSIKU | NTHAWI NDI CHIWERENGERO | MPHAMVU YAKE NDI UBWINO WAKE |
|---|---|---|---|
| 1 | **Ayatul Kursi (2:255)** | M'mawa, madzulo, asanagone ndi pambuyo pa Swalaat ya Fardh | Satana sangamuyandikire iye, ndichifukwanso chokalowera ku Jannat. |
| 2 | **Surat 2:285 – 286** | Madzulo komanso asanagone | Zidzamteteza ku choipa cha zilizonse. |
| 3 | **Surat zitatu Ikhlas, Falaq ndi Nas** | Katatu m'mawa, katatu madzulo | Zidzamteteza ku chilichonse |

| | | | |
|---|---|---|---|
| 4 | ( بسم الله الذي لا يضر مع اسمه شيء في الأرض ولا في السماء وهو السميع العليم)[1] | Katatu m’mawa, katatu madzulo | Sangampeze mavuto mwa dzidzidzi, komanso sichingampatse vuto chilichonse. |
| 5 | (أعوذ بكلمات الله التامات من شر ما خلق)[2] | Katatu madzulo, ndi amene wafika panyumba. | Tchingo la malo ku vuto lililonse. |
| 6 | ( حسبي الله لا إله إلا هو عليه توكلت وهو رب العرش العظيم )[3] | Kasanu ndi kawiri m’mawa, komanso kasanu ndi kawiri madzulo. | Allah adzamkwaniritsa udindo umene wampatsa pa zinthu za duniya ndiku Aakhirat. |
| 7 | ( رضيت بالله ربًا، وبالاسلام دينًا، وبمحمد ﷺ نبيًا)[4] | Katatu m’mawa komanso katatu madzulo. | Udzakhala udindo wa Allah kuti amusangalatse iye. |
| 8 | (اللَّهُمَّ بك أصبحنا وبك أمسينا وبك نحيا وبك نموت وإليك النشور)[5] | Masana ndi madzulo. | Kwadza Hadith yolimbikitsa zimenezo. |
| 9 | ( أصبحنا على فطرة الإسلام، وكلمة الإخلاص، ودين نبينا محمد ﷺ وملة أبينا إبراهيم ﷺ حنيفًا مسلمًا وما كان من المشركين)[6] | Kum’mawa | Mneneri (SAW) anali kunena Du’aa imeneyi. |
| 10 | (اللَّهُمَّ مَا أَصْبَحَ بِي مِنْ نِعْمَةٍ أو باحَدٍ مِنْ خَلقِكَ فَمِنْكَ وَحْدَكَ لاَ شَرِيكَ لَكَ فَلَكَ الْحَمْدُ وَلَكَ الشُّكْرُ)[7] | Masana ndi madzulo. | Wakwaniritsa kuthokoza kwa tsiku lake ndi usiku wake. |
| 11 | ( اللهُمّ إنِيْ أصْبَحْتُ أشْهِدُكَ وَاَشْهِدُ حَمَلَةَ عَرْشِكَ وَمَلاَئِكَتِكَ وَأنْبِيَائَكَ وَجَمِيْعِ خَلْقِكَ بِأنّكَ أنتَ اللّهُ لاَ إلٰه إلاّ أنتَ وَأنّ مُحَمَّدًا عَبْدُكَ وَرَسُوْلُكَ )[8] | Kanayi m’mawa, komanso kanayi madzulo. | Amene anganene mau amenewa kanayi Allah adzam’masula iye kumoto. |
| 12 | (اللَّهُمَّ فاطر السموات والارض عالم الغيب والشهادة رب كل شيء ومليكه أشهد أن لا إلٰه إلا أنت، أعوذ بك من شر نفسي ومن شر الشيطان وشركه وأن أقترف على نفسي سوءًا أو أجرَّه إلى مسلم)[9] | M’mawa, madzulo ndi pogona. | Idzamteteza ku manong’onong’on a Satana. |

[1] Mdzina la Allah Yemwe pamodzi ndi dzina Lake palibe chinthu chomwe chingapereke vuto pansi ngakhale kumwamba, ndipo Iye Ngwakumva kwambiri Wodziwa kwambiri.

[2] Ndikudzitchinjiriza ndi mau a Allah okwanira ku zoipa zomwe analenga.

[3] Wandikwanira Allah, palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma Iye,ndayedzamira mwa Iye, ndipo Iye ndi Mwini mpando wachifumu wolemekezeka.

[4] Ndasangalatsidwa ndi Allah kukhala Mbuye wanga, ndinso Chisilamu kukhala Deen yanga, komanso Muhammad kukhhala Mneneri wanga.

[5] "E, Allah! Kudzera mwa Inu kwatichera, ndiponso kudzera mwa Inu kwatidera, ndiponso kudzera mwa Inu tikukhala moyo, ndinso kudzera mwa Inu tidzamwalira, komanso tidzaukitsidwa ndikubwera kwa Inu", ndipo madzulo anene kuti, "E, Allah! Kudzera mwa Inu kwatidera, ndiponso kudzera mwa Inu kutichera, ndinso kudzera mwa Inu tikukhala moyo, komanso kudzera mwa Inu timwalira, ndiponso kwa Inu ndikothera".

[6] Kwatichera tili pa Deen ya Chisilamu, pa liwu la Ikhlas, pa Deen ya Mneneri wathu Muhammad (SAW), komanso pa Deen ya kholo lathu Ibrahim (AS) mwangwiro modzipereka, ndipo sanali mwa opembedza mafano.

[7]"E, Allah! Mtendere ulionse omwe ndacheredwa nawo ine kapena ndi wina aliyense mu zolengedwa Zanu wochokera kwa Inu Nokha basi Mulibe wothandizana naye, choncho kutamandika konse ndi Kwanu, kuthokozedwanso ndi Kwanu. "Ndipo madzulo adzanena kuti Mtendere omwe ndaderedwa nawo kapena "

[8]"E, Allah! Kwandichera ine ndikukuchitani Inuyo, Amene anyamula mpando Wanu wachifumu, Angero Anu, Aneneri Anu ndi zolengedwa Zanu zonse kukhala mboni zanga kuti Inu Ndinu Allah palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma Inu, ndikuti Muhammad ndi kapolo Wanu komanso Mtumiki Wanu. "Ndipo nthawi yamadzulo adzanena Du’aa imeneyi moyamika ndi mau akuti, kwandidera"

[9]E, Allah! Mlengi wakumwamba ndi pansi, Wodziwa za nseli ndi zoonekera, Mwini chilichonse komanso Mfumu Yake, ndikuikira umboni kuti palibe wopembedzedwa mwachoonadi koma Inu, ndikudzitchinjiriza mwa Inu ku zoipa za moyo wanga, ndinso ku zoipa za Satana ndi gulu lake, ndikuti ndidzichitire zoipa kapena kuti ndizikokere zoipazo kwa Msilamu.

| | | | |
|---|---|---|---|
| 13 | (اللَّهُمَّ إني أعوذ بك من الهم والحزن وأعوذ بك من العجز والكسل وأعوذ بك من الجبن والبخل وأعوذ بك من غلبة الدين وقهر الرجال) [1] | Kum'mawa kamodzi, komanso kumadzulo kamodzi. | Adzathetsa maganizo ndi madandaulo ake, komanso ngongole yake idzabwezedwa. |
| 14 | (اللَّهُمَّ أَنْتَ رَبِّي لَا إِلَهَ إِلَّا أَنْتَ خَلَقْتَنِي وَأَنَا عَبْدُكَ وَأَنَا عَلَى عَهْدِكَ وَوَعْدِكَ مَا اسْتَطَعْتُ أَعُوذُ بِكَ مِنْ شَرِّ مَا صَنَعْتُ أَبُوءُ لَكَ بِنِعْمَتِكَ عَلَيَّ وَأَبُوءُ لَكَ بِذَنْبِي فَاغْفِرْ لِي فَإِنَّهُ لَا يَغْفِرُ الذُّنُوبَ إِلَّا أَنْتَ) [2] | Mauwa ndi bwana wa Istighfaar, anenedwe m'mawa ndi madzulo. | Amene anganene mauwa mowakhulupirira munthawi ya masana namwalira mu usana wa tsiku limenelo, kapena awanena usiku namwalira mu usiku umenewo ndiye kuti ameneyo ali mgulu la anthu aku Jannat. |
| 15 | (يا حي يا قيوم برحمتك أستغيث أصلح لي شاني كله ولا تكِلني إلى نفسي طرفة عين) [3] | M'mawa ndi madzulo. | Mneneri (SAW) anamulangiza bibi Fatimah kutero. |
| 16 | (اللَّهُمَّ عافني في بدني، اللَّهُمَّ عافني في سمعي، اللَّهُمَّ عافني في بصري، اللَّهُمَّ إني أعوذ بك من الكفر والفقر، اللَّهُمَّ إني أعوذ بك من عذاب القبر لا إلٰه إلا أنت) [4] | Katatu m'mawa komanso katatu madzulo. | Kwadza mau kuti Mneneri (SAW) anali kuchita Du'aa imeneyi. |
| 17 | (اللَّهُمَّ إني أسالكَ العفو والعافية في الدنيا والآخرة، اللَّهُمَّ إني أسألكَ العَافيةَ في ديني ودنيايَ وأَهْلي ومالي، اللَّهُمَّ اسْترْ عوْراتي وآمِنْ رَوْعاتي، اللَّهُمَّ احْفظني منْ بين يديَّ ومن خَلْفي وعن يميني وعن شمالي ومنْ فوْقي وَأَعوذُ بعظمتك أن أُغتالَ منْ تحْتي) [5] | M'mawa ndi madzulo. | Mtumiki wa Allah (SAW) sanali kuwasiya mau amenewa kukamamdera komanso kukamamchera. |
| 18 | (سبحان الله وبحمده عدد خلقه، ورضا نفسه، وزنة عرشه، ومداد كلماته) [6] | Katatu M'mawa. | Kunena mau amenewa ndibwino kwambiri kuposa kukhala pansi ndikumachita zikr kuyambira fajr mpaka masana. |

[1] E, Mbuye wanga! Ine ndikudzitchinjiriza mwa Inu ku maganizo ndi madandaulo, ndikudzitchinjirizanso mwa Inu ku kulephera ndi ulesi, ndikudzitchinjirizanso mwa Inu ku mantha ndi umbombo, komanso ndikudzitchinjiriza mwa Inu ku kupanikizika ndi ngongole, ndinso ku ukali wa anthu.

[2] E, Allah! Ndinu Mbuye wanga! Palibe wopembedzedwa mwachoonadi koma Inu, munandilenga ine, ndipo ndine kapolo Wanu, ndili pa pangano ndi lonjezo Lanu m'mene ndingathere, ndikudzitchinjiriza mwa Inu ku zoipa zomwe ndachita, ndikubwerera kwa Inu kudzera mu mtendere Wanu umene mwandipatsa komanso polapa machimo anga, choncho ndikhululukireni, pakuti palibe amene angakhululuke machimo koma Inu.

[3] E, Inu Amoyo, M'yang'aniri! Ndikupempha chipulumutso kudzera mchisoni Chanu, ndikonzereni zochitika zanga zonse, musandilekerere ndekha ngakhale kamphindi konga kuphethira kwa diso.

[4] E, Mbuye wanga! Ndipatseni thupi lathanzi, makutu a thanzi, ndi maso a thanzi, E, Mbuye wanga! Ine ndikudzitchinjiriza mwa Inu ku ukafiri komanso umphawi, E, Mbuye wanga! Ine ndikudzitchinjiriza mwa Inu ku chilango cha manda, palibe wopembedzedwa mwachoonadi koma Inu.

[5] E, Mbuye wanga! Ine ndikukupemphani moyo wathanzi pa Deen yanga, pa zinthu zanga za duniya, pa banja langa ndi pa chuma changa, E, Allah! Bisani umaliseche wanga ndikundichotsera mantha anga, E, Mbuye wanga! Nditetezeni ku zapatsogolo panga, zapambuyo panga, zakumanja kwanga, zakumanzere kwanga ndi zakumwamba kwanga, komanso ndikudzitchinjiriza kudzera mu ulemerero Wanu kuti ndisachitiridwe chiwembu kuchokera pansi panga.

[6] Kuyera ndikwa Allah komanso atamandike m'mene zachulukira zolengedwa Zake, m'mene akufunira Iye, ngati kulemera kwa mpando Wake wachifumu, ndi ututo olembera mau Ake.

# ZOYANKHULA NDI ZOCHITIKA ZOMWE ZANENEDWA KUTI ZILI NDI MALIPIRO AKULU

| | MAU KAPENA NTCHITO YABWINO | MALIPIRO NDI SAWABU ZAKE KUCHOKERA MU SUNNAT, MNENERI (SAW) ANATI: |
|---|---|---|
| 1 | لا إله إلا الله وحده لا شريك له الملك وله الحمد وهو على كل شيئ قدير Palibe wopembedzedwa mwachoonadi koma Allah Yekhayo, Alibe wothandizana naye, Ali ndi ufumu komanso kutamandika, ndipo Iye ndi Wamphamvu pa chilichonse. | Amene anganene mau amenewa kokwanira zana limodzi pa tsiku adzakhala ndi sawabu zolingana ndi zakupereka ufulu kwa akapolo khumi, zidzalembedwa kwa iye zabwino zokwana zana limodzi, machimo ake okwana zana limodzi adzafufutidwa, ndipo mau amenewa adzakhala kwa iye mtsiriko ku Satana pa tsiku limenelo mpaka kum'dera, ndipo sanachite aliyense chabwino kwambiri kuposa chomwe iye wachita kupatula yekhayo amene wachulutsa kuchita zimenezo. |
| 2 | سبحان الله العظيم و بحمده SUB - HANALLAHIL ADHWIMI WABIHAMDIHI Chiyero ndi cha Allah Wolemekezeka ndi kutamandika Kwake. | Amene anganene kuti: SUBHANALLAHIL - ADHWIMI WABIHAMDIHI udzabzalidwa kwa iye mtengo wakanjedza ku Jannat |
| 3 | سبحان الله و بحمده سبحان الله العظيم Kuyera ndi kutamandika ndi za Allah. Kuyera ndi kutamandika Kwake ndi za Allah chiyero ndicha Allah Wamkulu. | Munthu amene anganene pamene kukum'chera ndi pamene kukum'dera kuti: "SUB – HANALLAHI WABIHAMDIHI" kokwanira zana limodzi adzakhululukidwa machimo ake ngakhale atachuluka ngati thovu la m'nyanja, ndipo pa tsiku la Kiyaamat palibe amene adzabweretse zabwino kwambiri kuposa zomwe iye adzabweretse, kupatula yekhayo amene ananena ngati zomwe iye ananena kapena kuonjezera. "Pali mau awiri opepuka pa lirime, olemera pa sikelo, okondedwa kwa Allah: SUB-HANALLAHI WABIHAMDIHI, SUB-HANALLAHIL-ADHWIMI". |
| 4 | LA HAULA WALAA QUWWATA ILLA BILLAH | "Kodi ndikusonyeze nkhokwe, m'nkhokwe za ku Jannat? Ndipo ine ndinati, Inde, Mtumiki (SAW) anati: "Kunena mau oti: LAA HAULA WALAA QUWWATA ILLA BILLAH" |
| 5 | KUPEMPHA JANNAT NDIKUDZITCHIN JIRIZA KU MOTO | "Yemwe angapemphe Jannat kokwanira katatu, Jannat imayankhula kuti Oh Allah kamulowetseni ku Jannat. Ndipo munthu amene angapemphe kupulumutsidwa ku moto, moto umanena kuti Oh Allah mupulumutseni ku moto". |
| 6 | Dipo la pa bwalo | Amene wakhala pa bwalo ndi kuchulukapo phokoso ndipo n'kunena asananyamuke pa bwalo limenelo kuti: "SUB - HANAKALLAHUMMA WABIHAMDIKA, ASH - HADU AN LAA ILAAHA ILLA ANTA, ASTAGHFIRUKA WA ATUUBU ILAIKA" - Kuyera ndi kwanu E, Mbuye wanga ndi kutamandika Kwanu, ndikuikira umboni kuti palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma Inu, ndikukupemphani chikhululuko komanso ndikulapa kwa Inu - pokhapokha adzakhululukidwa machimo omwe anachita pomwe anakhalapo." |
| 7 | Kusunga pa mtima ma ayat a mu Surat Kahf | Amene wasunga pa mtima ma Ayat khumi oyambirira a Surat Kahf adzatetezedwa kwa Dajjaal |
| 8 | SWALAATU ALANNABI (kumufunira zabwino Mneneri) | "Amene wandifunira zabwino kamodzi Allah adzam'patsa madalitso okwanira khumi, ndipo adzakhululukidwa machimo ake okwana khumi, ndipo adzatukulidwa kwa iye ma ulemerero khumi". Ndipo mu Hadith ina akunena kuti: "Ndipo zidzalembedwa kwa iye chifukwa cha Swaliyatume imodziyo sawabu zokwana khumi." |

| | | |
|---|---|---|
| 9 | Kuwerenga ma Surat ena ndi ma Ayat ena a mu Quran | Amene angawerenge usana ndi usiku ma Ayat makumi asanu sangalembedwe m’gulu la anthu onyalanyaza, ndipo amene wawerenga ma Ayat zana limodzi adzalembedwa m’gulu la anthu odzichepetsa, amene wawerenga ma Ayat mazana awiri Qur'an sikalimbana ndi iye pa tsiku la Kiyaamat, ndipo amene wawerenga ma Ayat mazana asanu, adzalipidwa milu ya malipiro. |
| 10 | Malipiro a ochita Azaan | "Ndithu majini kapena anthu kapenanso chilichonse sangamve pothera liwu la Mu - azzin koma aliyense wa iwo adzamuikira umboni iye pa tsiku la Kiyaamat" "Ochita Azaan pa tsiku la Kiyaamat adzakhala ataliatali makosi kuposa anthu onse”. |
| 11 | Kutsatizana ndi Mu - azzin pamene akuchita Azaan, ndikuchita Du'aa pambuyo pa Azaan | Munthu amene anganene Du'aa iyi akumva Azaan .................. "E, Mbuye wathu Mwini kuitana kwa chikwanekwaneku, ndi Swalaat yamuyaya, m’patseni Muhammad (SAW) Wasilat ndi ulemerero, ndipo mukamudzutse pa malo wotamandika womwe mudamulonjeza pa tsiku la Kiyaamat” pokhapokha Du'aa yanga idzampeza iye" |
| 12 | Kulongosola wudhu | Amene wachita wudhu naulongosola machimo ake adzatuluka m’thupi mwake mpakanso pansi kwa makadabo ake |
| 13 | Du'aa pambuyo pa wudhu | "Palibe mmodzi wa inu amene angachite wudhu ndikulongosola bwinobwino, kenako nanena kuti: “ASH - HADU AN LA ILAHA ILLAH, WA ASHHADU ANNA MUHAMMADAN ABDUHU WARASULUH” - Koma adzatsegulidwa kwa iye makomo asanu ndi atatu a Jannat ndipo adzalowera khomo lililonse adzafune" |
| 14 | Kuswali marakaat awiri pambuyo pa wudhu | Palibe Msilamu amene angapange wudhu naulongosola wudhu wakewo, kenako naima kuswali marakaat awiri mowalunjika marakaat awiriwo ndi mtima wake komanso nkhope yake (kwa Allah), koma kuti Jannat ikakhala Waajib kwa iye kukailowa |
| 15 | Kuyenda mapazi ochuluka popita ku mzikiti | Amene wapita ku mzikiti wa Jamaat, phazi lililonse limafufuta tchimo, ndipo phazi lililonse amalipidwa nalo sawabu imodzi popita ndi pobwerera |
| 16 | Kukonzekera ndi kulawirira ku Swalaat ya Jumuat | "Amene wachapa tsiku la Jumuat nasamba, kenako nafuna kulawirira, nalawirira, ndikuyenda wapansi osayenda pa chokwera, namuyandikira Imaam, namvetsera zimene akunena, ndipo sanachite zamasewera; ndiye kuti pa phazi lililonse kwa iye adzapeza malipiro a ntchito ya chaka chatunthu, monga malipiro a kumanga chaka chonse ndi kuswali chaka chonse."<br>"Sangasambe munthu wamwamuna tsiku la Jumuat, nadziyeretsa m'mene angathere, nadzola mafuta ake, kapena kudzinunkhiritsa ndi mafuta a m’nyumba mwake, kenako n'kutuluka ulendo ku Jumuat, napanda kusiyanitsa pakati pa anthu awiri, kenako naswali zomwe walamulidwa kuti aswali, nakhala chete kumvetsera Imaam akayamba Khutbat, ndiye kuti iye adzakhululukidwa machimo omwe ali pakati pa tsiku limeneli ndi Jumuat yam'mbuyo." |
| 17 | Kuyipeza Takbirat ya Ihraam | "Amene waswali pa Jamaat kuti Allah amukonde kwa masiku makumi anayi akuyipeza Takbirat yoyamba ndiye kuti kudzalembedwa kwa iye kudzitalikitsa kuwiri: kudzitalikitsa ku moto ndi kudzitalikitsa ku uchiphamaso." |
| 18 | Kuswali Fardh pa Jamaat | "Swalaat ya pa Jamaat imapambana Swalaat ya payekha ndi maulemerero makumi awiri mphambu zisanu ndi ziwiri." |

| | | |
|---|---|---|
| 19 | Kuswali Isha ndi Fajr pa Jamaat | "Amene angaswali Isha pa Jamaat ali ngati waswali theka la usiku, ndipo amene waswali Subhi pa Jamaat ali ngati waswali usiku wonse." |
| 20 | Kuswali mu swafa yoyamba | "Anthu akanakhala kuti akudziwa sawabu zomwe zili pakuchita Azaan ndi kuswali mu swafa yoyamba ndipo sanapeze mwayi wotero pokhapokha atachita mayere kuti zitero bwenzi akuchita mayere." |
| 21 | Kusamala Sunnat zotsatizidwa ndi Fardh | "Amene angaswali usiku ndi usana marakaat khumi ndi awiri adzamangiridwa nyumba ku Jannat; marakaat anayi asanaswali Zuhr, komanso marakaat awiari pambuyo pa Zuhr, marakaat awiri pambuyo pa Maghrib, marakaat awiri pambuyo pa Ishat ndi marakaat awiri asanaswali Fajr." |
| 22 | Kuchulutsa ma Sunnat a Swalaat | "Uzichulutsa kumulambira Allah, pakuti iwe sungamulambire Allah ndi sajdat imodzi koma Allah adzakutukulira ndi sajdat imeneyo ulemerero, ndi kukuchotsera ndi sajdatyo tchimo." |
| 23 | Sunnat asanaswali Fajr ndi Fardh ya Fajr | "Marakaat awiri a patsogolo pa Fajr ndi opambana kwambiri kuposa duniya ndi zomwe zili m'menemo",<br>"Amene waswali Subh ndiye kuti ameneyo ali m'manja mwa Allah" |
| 24 | Swalaat ya Dhuha | "Chiwalo cha aliyense wa inu chimam'chera kukhala sadaka, choncho Tasbihi iliyonse ndi sadaka, Tahmidi iliyonse ndi sadaka, tahlili iliyonse ndi sadaka, Takbirat iliyonse ndi sadaka, kulamulira zabwino ndi sadaka, ndiponso kuletsa zoipa ndi sadaka, ndipo zimenezo zikwaniritsidwa ndi marakaat awiri amene angawaswali nthawi ya Dhuha yomwe ndi nthawi yakum'mawa. |
| 25 | Amene wakhala pa malo pake poswalira namachita Zikr | "Angero amam'chitira Du'aa mmodzi wa inu pa nthawi imene ali pa malo pake poswalira ngati wudhu wake sunaononongeke ponena kuti: "E, Allah! M'khululukireni, E, Allah! M'chitireni chisoni." |
| 26 | Kuchita Zikr pambuyo poswali Fajr pa Jamaat mpaka kutuluka kwa dzuwa, kenako n'kuswali marakaat awiri | "Amene waswali Subh pa Jamaat kenako n'kukhala n'kumam'kumbukira Allah mpaka kutuluka dzuwa naswali marakaat awiri adzapeza sawabu ngati malipiro a Hajj ndi Umrat zachikwanekwane." |
| 27 | Amene wadzuka usiku kuti aswali namudzutsa mkazi wake | "Amene wadzuka usiku namudzutsa mkazi wake awiriwo nkuswali marakaat awiri limodzi, adzalembedwa m'gulu la anthu achimuna ndi achikazi om'kumbukira Allah kwambiri." |
| 28 | Amene watsimikiza zoswali usiku nagonjetsedwa ndi tulo | "Palibe munthu amene angakhale ndi Niyyat yoswali usiku nalephera kuswaliko chifukwa chogonjetsedwa ndi tulo, koma Allah adzamulembera iye malipiro a Swalaat yake ndipo tulo take timeneto tidzakhala sadaka." |
| 29 | Duwa ya munthu walowa mu msika | "Laa ilaaha illa Allah Wahdahuu laa shariika lahu, lahul mulk walahul hamdu yuhyii wayumiitu, wahuwa hayyun laa yamuutu biyadihil khairu wahuwa alaa kulli shain qadiir". Allah amamulembera iyeyo zabwino zikwi chikwi chimodzi (1,000,000) ndipo amamufufutira zoipa zikwi chimodzi (1,000,000) ndipo amamutukulira masitepe okwanira zikwi chikwi chimodzi (1,000,000). |
| 30 | Kunena mau oti SUB - HANALLAH, WALHAMDULILLAH, WALLAHUAKBAR, ka | "Amene anganene mau oti: SUB - HANALLAH, kumapeto kwa Swalaat iliyonse ka (33), AL HAMDU LILLAH, ka (33) komanso ALLAHU AKBAR ka (33), motero kameneko n'kukhala (99) nakwaniritsa ka (100). Ponena mau oti, LA |

| | | |
|---|---|---|
| | (33), ndikumamalizira ndi mau oti LA ILAHA ILLALLAH, kumapeto kwa Swalaat ya Fardh | ILAHA ILLALLAHU WAH DAHU LA SHARIKA LAHU, LAHUL MULKU WALAHUL HAMDU, WAHUWA ALA KULLI SHAI - IN QADEER, machimo ake adzakhululukidwa ngakhale anali ochuluka ngati thovu la m,nyanja." |
| 31 | Kuwerenga Ayatul kursi kumapeto kwa Swalaat ya Fardh | "Amene angawerenge Ayatul kursi kumapeto kwa Swalaat iliyonse ya Fardh palibe chimene chingamuletse kukalowa ku Jannat kupatula imfa." |
| 32 | Kuzonda matenda | "Palibe Msilamu aliyense amene angamuzonde Msilamu amene akudwala nthawi ya kum'mawa koma Angero zikwi makumi asanu ndi awiri (70,000) amam'chitira Du'aa iye mpaka madzulo, ndipo ngati atakamuzonda mu nthawi ya madzulo angero zikwi makumi asanu ndi awiri (70,000) amam'chitira Du'aa iye mpaka mmawa, ndipo ku Jannat akakhala ndi zipatso za tende." |
| 33 | Duwa ya yemwe wapatsidwa mayeserero | Munthu amene wamuona munthu amene ali m'mayeserero nanena kuti: "Alhamdu lillaahi llazii aafaanii mimmaa butalaaka bihi wafaddhwalani alaa kathiirin mimman khalaqa tafdhwiilan" sangam'peze mayeserero amenewo. |
| 34 | Chipepeso | "Amene angam'pepese munthu amene ali pa vuto, iyenso adzapeza malipiro onga a iye."<br>"Palibe munthu wokhulupirira aliyense amene angam'pepese m'bale wake pa vuto lomwe ali nalo koma Allah adzam'veka iye zovala za ulemerero." |
| 35 | Kuswalira Janazat kenako n'kuitsatira wakumanda mpaka ataikidwa | "Amene wafika pa maliro mpaka ataswalira nawo, adzapeza Qeeraat, ndipo amene wafika ku maliro mpaka kuikidwa m'manda adzapeza ma Qeerat awiri, panafunsidwa kuti kodi ma Qeerat awiriwo ndi chiyani? Mtumiki (SAW) anati "Sawabu zochuluka ngati mapiri awiri akuluakulu." Ibn Umar (RA) ananena kuti "Ndithu tawalephera ma Qeeraat ambiri." |
| 36 | Kumanga mzikiti ndi cholinga chomusangalatsa Allah | "Amene wamanga mzikiti ndi cholinga chomusangalatsa Allah ngakhale utakhala wochepa ngati chisa cha mbalame, Allah adzam'mangira iye nyumba ku Jannat." |
| 37 | Kupereka pa njira ya Allah | "Palibe tsiku lomwe munthu amacheredwa koma Angero awiri amatsika ndipo mmodzi wa awiriwo amanena kuti E, Allah! M'patseni wopereka zina pamene wachotsapo, ndipo wina amati, E, Allah! M'patseni womana chionongeko." |
| 38 | Sadaka | "Sadaka palibe pamene imapungula chuma, ndipo palibe chimene Allah angaonjezere kwa munthu atapereka zotsala koma ulemerero, palibe amene angadzichepetse ndi cholinga chomusangalatsa Allah koma Allah amam'tukula iye pa ulemerero."<br>"Dirham imodzi idaposa (100,000) Dirham. Maswahaaba (RA) anati E, Inu Mtumiki wa Allah motani? Mtumiki (SAW) anati: 'Munthu wina anali ndi ma Dirham awiri, choncho watenga imodzi mwa awiriwo napereka sadaka, ndipo munthu wina ali ndi chuma chambiri, choncho watenga kuchokera mu katundu wa chuma chake ndalama zokwana(100,000) Dirham ndipo wachitira Sadaka."<br>"Palibe Msilamu amene angadzale mtengo kapena kulima mbewu, n'kumadyamo mbalame kapena munthu kapena nyama pokhapokha chimenecho kwa iye chimakhala sadaka" |
| 39 | Kukongoza mosafuna phindu | "Palibe Msilamu amene angam'kongoze Msilamu wina ngongole kokwanira kawiri koma adzakhala ngati kuti ngongoleyo wachitira |

| | | |
|---|---|---|
| | | sadaka kamodzi." |
| 40 | Kumukhulukira amene akulephera kubweza ngongole | "Munthu wina anali kuwakongoza anthu ndipo anali kumuuza mnyamata wake kuti ukafika kwa munthu amene akulephera kubweza ngongole ukam'khululukire mwina Allah adzatikhululukira, anati atakakumana ndi Allah, anam'khululukira." |
| 41 | Kumanga (kusala) tsiku limodzi pa njira ya Allah | "Amene angamange tsiku limodzi pa njira ya Allah, Allah adzaitalikitsa nkhope yake ndi moto pa mtunda wokwana kuyenda zaka makumi asanu ndi awiri." |
| 42 | Kumanga (kusala) masiku atatu m'mwezi uli onse, tsiku la Arafat ndi tsiku la Aashuraa | "Kumanga masiku atatu m'mwezi ulionse, komanso Ramadhan mpaka Ramadhan ina, sawabu zake ndi zochuluka ngati za kumanga chaka chatunthu, ndipo anafunsidwa za kumanga tsiku la Arafat, ndipo Mtumiki (SAW) poyankha anati: " Kumafafaniza machimo a kumene kwapita kwa chaka ndi kumene kwatsala." Ndipo anafunsidwa za kumanga tsiku la Aashuraa, ndipo anati kumafafaniza machimo a chaka chatha." |
| 43 | Kumanga masiku asanu nd limodzi m'masiku a Shawwal | "Amene wamanga mwezi wa Ramadhan natsatiza masiku asanu ndi limodzi a m'mwezi wa Shawwaal adzakhala ngati wamanga chaka". |
| 44 | Kuswali Taraweeh pamodzi ndi Imaam mpaka kumaliza | "Ndithu munthu akaswali pamodzi ndi Imaaam mpaka kuchoka atamaliza zidzawerengedwa kwa iye kuti waswali usiku wonse." |
| 45 | Umrat ya m'mwezi wa Ramadhaan | "Umrat ya m'mwezi wa Ramadhan sawabu zake zimalingana ndi za Hajj, kapena sawabu za Hajj yochita pamodzi ndi ine." |
| 46 | Hajj yabwino | "Amene wachita Hajj n'cholinga chomusangalatsa Allah ndipo sanayankhule mau oipa, kapena kupandukira chilamulo, adzabwerera alibe machimo ngati tsiku limene anam'bala."<br>" Ndipo Hajj yabwino ilibe mphoto ina koma Jannat" |
| 47 | Ntchito yabwino yochitika mu khumi loyambirira m'mwezi wa Dhul hijjah | "Palibe masiku abwino kuwachitiramo ntchito yabwino yomwe ili yabwino kwambiri kwa Allah kuposa masiku amenewa, masiku khumi oyambirira a Dhul Hijjat. Maswahaaba anafunsa kuti: 'Ngakhale kuchita Jihaad pa njira ya Allah ?' Mtumiki (SAW) anati: "Ngakhale kuchita Jihaad pa njira ya Allah, kupatula munthu amene watuluka mwini wakeyo ndi chuma chake ndipo sanabwerere ku nkhondoko ndi kalikonse." |
| 48 | Qurbaan | "Maswahaaba a Mtumiki wa Allah (SAW) anafunsa kuti: 'E, inu Mtumiki wa Allah! Kodi ma Qurban amenewa ndi ati?' Mtumiki (SAW) anati: "Imeneyi ndi Sunnat ya bambo wanu Ibraham". Anafunsa kuti: " E, inu Mtumiki wa Allah! Ife tipezamo chiyani?" Mtumiki (SAW) anati: "Tsitsi lililonse la nyama lili ndi Sawabu. "Anafunsanso kuti: 'E, inu Mtumiki wa Allah! Ubweyanso?' Mtumiki (SAW) anati: "Tsitsi la ubweya ulionse lili ndi Sawabu." |
| 49 | Malipiro a Aalim ndi ulemerero wake | "Ulemerero wa Aalim pa munthu wopembedza chabe uli ngati ulemerero wanga pa amene ali wapansi mwa inu, kenako Mtumiki wa Allah (SAW) ananena kuti: " Ndithu Allah, Angero Ake ndi akumwamba ndi pansi mpaka nyerere zomwe zili m'mabowo mwake, komanso nsomba zimam'funira zabwino wophunzitsa anthu." |
| 50 | Kupempha Allah zofera pa njira Yake m'choonadi | "Amene wam'pempha Allah zofera pa njira Yake m'choonadi Allah adzakamuukitsa pa maulemerero a mashaheed ngakhale atafera pa malo ake wogona." |

| | | |
|---|---|---|
| 51 | Kulira chifukwa chomuopa Allah ndi kulondera mu njira Yake | "Maso awiri sakakhudzidwa ndi moto; Diso lomwe linalira chifukwa chomuopa Allah, ndi Diso lomwe linachezera pa kulondera m'njira ya Allah." |
| 52 | Kuyedzamira mwa Allah, kusiya kudzilemba ndi chitsulo cha moto, kusiya kupempha maduwa amachiritso komanso kuombeza ndi mbalame | " Mneneri (SAW) anaonetsedwa ma ummat kutulo , ndipo anaona ummat wake , anthu zikwi makumi asanu ndi awiri , (70,000) mwa iwo akulowa ku Jannat mopanda kuwerengedwa ntchito zawo ngakhale kulangidwa, ndipo amenewo ndi amene sadzilemba ndi zitsulo za moto sagwiritsa ntchito maduwa amachiritso, saombezanso ndi mbalame , ndipo amayedzamira pa Mbuye wao." |
| 53 | Malipiro a yemwe ana ake ang'ono amwalira | "Mwa anthu mulibe Msilamu amene angamwalire ana ake atatu amene sanafike potha msinkhu napirira koma Allah akamulowetsa iye ku Jannat." |
| 54 | Kusiya kuona ndikupirira | "Ndithu Allah wanena kuti: "Ndikamuyesa kapolo wanga pomuchotsera zokondedwa zake ziwiri zomwe ndi maso, napirira, m'malo mwake ndidzamulipira Jannat." |
| 55 | Kusiya chinthu chifukwa chomuopa Allah | "Ndithu iwe sungasiye chinthu chifukwa chomuopa Allah koma adzakupatsa chinthu chabwino kuposa chimenecho." |
| 56 | Kusamala maliseche komanso lirime | " Amene anditsimikzire ine zosamalira chomwe chili pakati pa masaya ake awiri chomwe ndi lirime, komanso chomwe chili pakati pa miyendo yake iwiri, maliseche, ndikumutsimikizira kuti akalowa ku Jannat" |
| 57 | Kunena Tasmiyat polowa m'nyumba ndi pakudya | "Munthu akafuna kulowa m'nyumba mwake namutchula Allah akamalowamo, komanso akafuna kudya , Satana amanena kuti mulibe malo wogona ngakhale chakudya cha madzulo, ndipo akalowa napanda kumutchula Allah pamene akulowa, Satana amanena kuti mwapeza malo wogona komanso chakudya cha usiku." |
| 58 | Kum'tamanda Allah pambuyo pa kudya , kumwa ndi povala chovala chatsopano | " Amene wadya chakudya nanena kuti: "AL HAMDU LIL LAHILLADHI AT- AMANI HADHA WARAZAQANEEHU MIN-GHAIRI HAULIN MINNI WALAA QUW-WAT" (kutamandika konse ndi kwa Allah Amene wandipatsa chakudyachi, mopanda nzeru yochokera kwa ine ngakhale mphamvu) amakhululukidwa machimo ake a m'mbuyo. Ndipo akamwa chakumwa anene kuti: "AL HAMDU LILLAHILLADHI SA QAANI HADHA" (Kutamandika konse ndi kwa Allah Amene wandipatsa chakumwachi) ndipo akavala nsalu yatsopano anene kuti: "AL HAMDU LILLAHILLADHI KASAANI HADHA" " Kutamandika konse ndi kwa Allah Amene wandiveka nsaluyi " |
| 59 | Amene akufuna kuti Allah am'peputsire mavuto a ntchito yake | "BIBI Fatima (RA) anam'pempha Mtumiki (SAW) munthu wa ntchito, ndipo anati kwa Fatima ndi Ali (RA): "Kodi ndikuphunzitseni chinthu chabwino kuposa chimene mwandipemphachi? Mukafika pa malo anu wogona nenani Allahu Akbar ka (34), sub- hanAllahi ka (33). Ndiponso Alhamdu lillahi ka (33), kutero zilibwino kwambiri kwa inu kusiyana ndi munthu wa ntchito." |
| 60 | Duàa, mwamuna ndi mkazi asanayambe kugonana | " Ngati mmodzi wa iwo pamene akufuna kugonana ndi mkazi wake anena kuti," BISMILLAH, ALLAHUMMA JANNIB-NASH-SHAITWANA WAJANNIBISH-SHAITWANA MA RAZAQ-TANA" |

| | | |
|---|---|---|
| | | M'dzina la Allah, E, Allah! Tipewetseni Satana, ndikum'pewetsa pa chomwe mwatipatsa », ndithu ngati atapatsidwa mwana pakati pawo m'kugonana kumeneko ndiye kuti Satana sangam'chite kanthu mwana ameneyo mpaka kalekale." |
| 61 | Mkazi kumusangalatsa mwamuna wake | "Mkazi akaswali zipindi zake zisanu, namanga mwezi wake wa Ramadhan, nasunga maliseche ake, ndi kumumvera mwamuna wake akauzidwa kuti lowa ku Jannat kudzera khomo lililonse lomwe ungalifune mwa makomo a ku Jannat."<br>"Mkazi aliyense amene wamwalira mwamuna wake ali wosangalala ndi mkaziyo, mkazi ameneyo akalowa ku Jannat". |
| 62 | Kulumikiza chibale | "Amene angasangalatsidwe kuti Rizq lake litambasulidwe, ndikuti asaiwalidwe ngakhale atamwalira ayenera kuti alumikize chibale chake." |
| 63 | Kulera mwana wamasiye | "Ine ndi munthu wolera mwana wamasiye tikakhala limodzi ku Jannat chonchi, ndipo analozera ndi zala zake ziwiri, chamkombaphala ndi chapakati." |
| 64 | Khalidwe labwino | "Ndithu wokhulupirira amatha kupeza ulemerero wa amene akumanga n'kumaswali chifukwa cha khalidwe lake la bwino".<br>"Ndine mtsogoleri pokalowa nyumba yomwe ili pamwamba pa Jannat kwa amene khalidwe lake lili labwino." |
| 65 | Kuzichitira chisoni ndi chifundo zolengedwa | "Ndithu Allah amawachitira chifundo mwa akapolo Ake anthu amene ali achifundo (kwa anzawo). "Achitireni chifundo amene ali pa dziko lapansi, adzakuchitirani chifundo Amene ali kumwamba." |
| 66 | Kuwafunira zabwino Asilamu | "Mmodzi wa inu sangakhale wokhulupirira mpaka atamufunira zabwino m'bale wake zomwe amazikonda iye mwini. |
| 67 | Manyazi | "Manyazi sabweretsa chilichonse koma zabwino."<br>"Manyazi ndi gawo limodzi la Imaan.<br>"Zinthu zinayi zili m'gulu la ma Sunnat a Atumiki: manyazi, kudzinukhiritsa, kuchita miswak ndi kukwatira." |
| 68 | Kuyambirira salaam | "Munthu wina anadza kwa Mneneri (SAW) ndipo anati "Assalaam alaikum," Mneneri (SAW) anati: "Khumi." kenako anadza wina nanena kuti: "Assalaam alaikum warahmatullahi wabarakaattuh." Mneneri (SAW) anati: "Makumi atatu" amanena sawabu. |
| 69 | Kugwirana chanza nthawi yokumana | "Palibe Asilamu awiri amene angakumane nagwirana chanza koma amakhululukidwa machimo asanasiyane." |
| 70 | Kuteteza ulemu wa Msilamu | "Amene angateteze ulemu wa m'bale wake, pa tsiku la Kiyaamat Allah adzaubweza moto ku nkhope kwake." |
| 71 | Kuwakonda ndi kukhala nawo anthu ochita zabwino | "Iwe udzaukitsidwa limodzi ndi amene umam'konda." Anas (RA) anati: "Maswahaaba sanasangalalepo monga momwe anasangalalira ndi Hadith imeneyi." |
| 72 | Okondana chifukwa cha ulemerero wa Allah | "Allah ananena kuti: "Amene amakondana chifukwa cha ulemerero Wanga akapeza nsanja za noor (dangalira), Aneneri ndi mashaheed azikawasirira iwo." |
| 73 | Duwa yopempherera Asilamu | "Duwa ya munthu Msilamu yopempherera m'bale wake, iye kulibe, ndiyoyankhidwa. Pa mutu pake pamakhala mngero amene anaikidwa, moti nthawi ili yonse imene iye amapempherera zabwino m'bale wakeyo, amanena mngero amene anaikidwa pa iyeyo kuti: "Aamiin – |

| | | |
|---|---|---|
| | | Allah alandire, nawenso ukhale nazo zofanana ndi zimenezo” |
| 74 | Kuwapemphera makhululuko Asilamu achimuna ndi achikazi | "Amene angawapemphere makhululuko Asilamu achimuna ndi achikazi, Allah adzamulembera iye kwa Msilamu wachimuna ndi wachikazi aliyense sawabu." |
| 75 | Kuchotsa choipa pa njira | "Ndithu ndinamuona munthu akuyendayenda ku Jannat chifukwa cha mtengo womwe anaudula umene unali pa njira ndipo unali kuvutitsa anthu." |
| 76 | Kusiya kutsutsana komanso bodza | "Ndine mtsogoleri wa nyumba yomwe ili m'mphepete mwa Jannat, ya amene wasiya za kutsutsana ngakhale akunena zoona, komanso nyumba imene ili pakati pa Jannat ya amene wasiya bodza ngakhale ali wa nthabwala." |
| 77 | Kumeza ukali | "Amene wameza ukali pomwe iye angathe kuuchita Allah adzamuitana iye tsiku la Kiyaamat pamaso pa zolengedwa kuti adzauzidwe kuti asankhe mkazi wa ku Jannat amene angam’fune." |
| 78 | Kunena zabwino kapena zoipa | "Amene mwamunenera zabwino zake, Jannat ili waajib kwa iye kuti akailowe, ndipo amene mwamunenera zoipa moto uli waajib kwa iye kuti akaulowe, ndinu mboni za Allah pa dziko lapansi." |
| 79 | Kupereka mpumulo kwa Msilamu ndi kum’peputsira | "Amene angapereke mpumulo kwa Msilamu pomuchotsera vuto mwa mavuto a dziko la pansi, Allah adzam’patsa iye mpumulo pomuchotsera mavuto a tsiku la Kiyaamat , ndipo amene wam’peputsira iye pa vuto lake, Allah adzamupeputsira iye pa dziko lino lapansi ndi ku Aakhirat , ndipo amene angam'bise Msilamu pa zinthu za manyazi, Allah adzam'bisa iye pa dziko lino lapansi komanso ku Aakhirat, Allah amathandiza munthu ngati munthuyo amam’thandiza m'bale wake ." |
| 80 | Kutsogoza Aakhirat | "Amene ingakhale Aakhirat cholinga chake Allah adzamuikira kulemera kwake mu mtima mwake, ndipo adzamusonkhanitsira iye mgwirizano wake , ndipo duniya idzafika kwa iye ili yonyozeka," |
| 81 | Mtsogoleri wa chilungamo, mnyamata wabwino , kugwirizana ndi mizikiti ndi kukondana chifukwa cha Allah | ‘Anthu asanu ndi awiri (7) Allah adzawaika pansi pa mthunzi wake pa tsiku lopanda mthunzi kupatula mthunzi Wake basi: Mtsogoleri wachilungamo, mnyamata amene wakula akum’chitira iabaadat Mbuye wake, munthu amene mtima wake nthawi zonse umakhala m’mizikiti, anthu awiri amene akondana chifukwa cha Allah anakumana ndi kusiyana ali okondana, munthu amene waitanidwa ndi mkazi waulemerero wake komanso wokongola kuti achite naye zachisembwere ndipo iye nkuyankha kuti ine ndimamuopa Allah, munthu amene wapereka sadaka naibisa kufikira poti mkono wake wamanzere wosadziwa chomwe mkono wake wamanja wapereka ndi munthu amene wam’kumbukira Allah mwamseri nayamba kulira”. |
| 82 | Kupempha chikhululuko kwa Allah | “Munthu amene angadzikakamize kuchita istighfaar (kupempha chikhululuko), Allah amamuchitira pa vuto lili lonse potulukira, komanso padandaulo lili lonse potulukira, ndipo amamupatsa rizq kuchokera mu zinthu zimene samayembekezerera.” |

# ZINTHU ZOMWE KWAFIKA KULETSEDWA KU ZIMENEZO KOMANSO KUZICHITA

| NO | CHOLETSEDWA | MTUMIKI WA ALLAH (SAW) ANANENA KUTI....... |
|---|---|---|
| 1 | Kugwira ntchito modzionetsera kwa anthu | "Allah ananena kuti Ine sindisowa wothandizana naye , amene wagwira ntchito ndi kundiphatikizira ine ndi wina pa ntchitoyo ndidzamusiya ndi amene wandiphatikizira nayeyo." |
| 2 | Kukonza kunja ndikuwonongeka mkati | "Ndithudi ine ndikuwadziwa anthu amene adzabwere tsiku la Kiyaamat ndi zabwino zonga mapiri a Tihaamat kuyera ndipo Allah adzazichita kukhala fumbi lobalalika." Thaubaan adati: 'Eh iwe Mtumiki (SAW)! Tatiuza mbiri zawo kwa ife komanso uwatulutsire poyera kuti tisakhale mwa iwo tisakudziwa'. Mtumiki (SAW) adati: "Iwowotu ndithudi ndi abale anu ndiponso a khungu lanu lomweli, amatenga gawo lawo la mapemphero a usiku ngati m'mene inu mukuchitiramu koma iwo ndi anthu oti akakhala kwa okha (mseri) ndi zomwe Allah adaziletsa, amazichita." |
| 3 | Kudzikweza | "Amene ali ndi khalidwe lodzikweza mu mtima mwake, lolemera ngati kanyerere, sakalowa ku Jannat," |
| 4 | Kukoka nsalu | Kupyoza malire ndi nsalu, malaya ndi chilemba: "Yemwe wakoka nsalu modzikweza Allah sakamuyang'ana tsiku la kiyama." |
| 5 | Kaduka | "Pewani kaduka pakuti kaduka kamadya sawabu monga mmene moto umadyera nkhuni kapena anati udzu." |
| 6 | Katapira | "Mtumiki wa Allah (SAW) anam'temberera munthu wodya chuma cha katapira komanso woperekayo"<br>"Dirham imodzi yomwe munthu angadye iye akudziwa kuti ndi ya katapira, tchimo lake ndi loopsa kwambiri kuposa lochita chiwerewere kokwanira makumi atatu mphambu zisanu ndi limodzi (36)." |
| 7 | Chidakwa | "Chidakwa sichikalowa ku Jannat, ngakhale wokhulupirira za matsenga ngakhalenso wodula chibale." |
| 8 | Bodza | "Tsoka lili kwa amene amakamba nkhani ndi cholinga chowaseketsa nayo anthu n'kumanama, tsoka ndi lake, tsoka ndi lake." |
| 9 | Ukazitape | "Ndipo amene wamvetsera nkhani ya anthu ena pomwe iwo sakusangalatsidwa naye kuti amve nawo, kapena akumuthawa iye kuti asamve nawo ndiye kuti mtovu udzathiridwa m'khutu mwake pa tsiku la Kiyaamat |
| 10 | Ziboliboli kapena zithunzi | "Tsiku la Kiyaamat ndithu amene adzakhale ndi chilango chowawa mwa anthu onse ndi amene amasema ziboliboli ndi zojambula." " Angero salowa m'nyumba momwe muli galu ngakhalenso chojambula" |
| 11 | Kukhwirizira nkhani | "Okhwirizira nkhani sakalowa ku Jannat." |
| 12 | Kujeda | "Kodi mukudziwa kuti mjedo ndi chiyani? Maswahaaba (RA) anati:"Allah ndi Mtumiki Wake ndi amene akudziwa kwambiri .Mtumiki(SAW) anati , "Kunena kwanu pomunena m'bale wanu ndi chomwe chingamuyipire". Zinafunsidwa kuti: "Mukuona bwanji ngati chimene ndikunenacho mwa m'bale wangayo chilipo?" Mtumiki (SAW) anati: "Ngati chimene ukunenacho mwa iye chilipo ndiye kuti wamujeda, ndipo ngati mwa iye mulibe chimenecho ndiye kuti wamunamizira." |
| 13 | Kutembelera | "Kumutemberera Msilamu kuli ngati kumupha."<br>"Anthu okonda kutemberera sakapeza nawo mwayi wa Duàa ya Mtumiki (SAW), komanso sakakhala mboni pa tsiku la Kiyaamat." |

| | | |
|---|---|---|
| 14 | **Kufalitsa chinsinsi** | “Ndithu mwa anthu amene ati akakhale ndi malo woipitsitsa kwa Allah pa tsiku la Kiyaamat ndi munthu amene amagonanana ndi mkazi wake kenako n’kumafalitsa chinsinsi cha mkaziyo. |
| 15 | **Zonyansa** | “Ndithu oyipitsitsa mwa anthu malo wofikira kwa Allah pa tsiku la Kiyamaat ndi amene anthu amusiya pofuna kupewa zoipa zake”. |
| 16 | **Kumunena Msilamu kuti ndi Kafiri** | "Munthu aliyense amene angamunene m'bale wake kuti, E, iwe Kafiri (okanira mwa Allah) ndiye kuti mmodzi wa iwo adzabwerera ndi Ukafiri ngati zili m'mene waneneramo, ndipo ngati sizili choncho udzabwerera kwa iye." |
| 17 | **Kutchedwa ndi dzina losakhala la bambo** | "Amene wadzitcha ndi dzina losakhala la bambo wake iye akuwadziwa ndiye kuti Jannat ili Haraam kwa iye kukailowa." "Musamakhale anthu onyansidwa ndi abambo anu poti amene sangawafune abambo ake ndiye kuti ndi kafiri.." |
| 18 | **Kumuopseza Msilamu,** | “Sizololedwa kwa Msilamu kuopseza Msilamu.” “Munthu amene angaloze m’bale wake ndi chitsulo, ndithu angero amamutemberera kufikira iye atachitula pansi.” |
| 19 | **Kumupha wopempha chitetezo m'maiko a Chisilamu** | "Amene angamuphe munthu amene ali pa chipangano popanda chifukwa chake sakamva fungo la Jannat, ndithudi fungo la Jannat likamveka pa mtunda woyenda zaka zana limodzi." |
| 21 | **Kumutcha bwana munthu mchiphamaso ndi wopandukira chilamulo** | "Musanene kwa mchiphamaso kuti bwana, chifukwa ngati iye angakhale bwana ndiye kuti mwamukwiyitsa Mbuye wanu." |
| 22 | **Kuwachita chinyengo owayang'anira** | "Palibe munthu amene Allah angam’patse udindo wowayang'anira anthu ena namwalira tsiku limene angadzamwalire ali wachinyengo kwa anthu ake koma Allah adzaichita Haraam Jannat kwa iye kuti akailowe." |
| 23 | **Kuyankha mafunso mopanda kuzindikira** | "Amene angayankhe funso mopanda kuzindikira tchimo lake lidzakhala kwa amene wayankha funsolo." |
| 24 | **Kusiya Swalaat ya Jumuat mwa mphwayi** | "Amene angasiye Jumuat kokwana katatu moichitira mphwayi Allah amadinda chidindo pa mtima pake." |
| 25 | **Kuchitira ulesi kuswali komanso kusiiratu kutero** | "Pangano lomwe lili pakati pa ife ndi iwo ndikuswali, choncho amene angasiye kuswali ndiye kuti wachita ukafiri." "Pakati pa munthu ndi shirk pali kusiya Swalaat." |
| 26 | **Kudutsa patsogolo pa munthu akuswali** | "Akanadziwa amene akudutsa patsogolo pa yemwe akuswali kuti ndi chilango chanji adzapeze zikanakhala zopepuka kwa iye kuti aime malo amodzi kwa zaka makumi anayi kusiyana ndikuti adutse patsogolo pake." |
| 27 | **Kuvutitsa oswali** | "Amene wadya anyezi, adyo ndi kurraath (zofanana ndi adyo), asawayandikire malo omwe anthu akuswalira, pakuti angero amavutitsidwa ndi zomwe anthu amavutitsidwa nazo." |
| 28 | **Kulanda malo** | "Amene angadzidulire malo wochepa molanda, pa tsiku la Kiyaamat Allah adzam’pachika iye nthakayo pa khosi m’nthaka zisanu n'ziwiri." |
| 29 | **Mau omwe amam’kwiyitsa Allah** | "Ndithu munthu amatha kuyankhula liwu lom’kwiyitsa Allah lomwe iye sakuliganizira kuti lili ndi vuto , akagwera m'moto wa Jahannam chifukwa cha liwulo kwa zaka makumi asanu ndi awiri(70) |
| 30 | **Kuchulutsa kuyankhula zosakhala kumutchula Allah** | "Musamachulutse kuyankhula zosakhala kumutchula Allah, pakuti kuchulutsa kuyankhula zosakhala kumutchula Allah kumayambitsa kuuma mtima." |

| | | |
|---|---|---|
| 31 | **Kuyankhula mosasamala** | "Ndipo ndithu mwa inu amene ali wodanidwa kwambiri kwa ine, ndipo akakhala patali ndi ine pa tsiku la Kiyaamat ndi amene amasokosera, poyankhula mosasamala ndi wochulutsa zoyankhula." |
| 32 | **Kuchitira ulesi kumukumbukira Allah** | "Palibe pamene angakhale anthu pa malo ndipo iwo napanda kumutchula Allah komanso wosamupempherera zabwino Mtumiki (SAW) pokhapokha pamakhala chionongeko pa iwo. Ndipo Allah akafuna akawalanga komanso akakafuna akawakhululukira." |
| 33 | **Kuonetsera kusangalala ndi kunyogodola pa tchimo la Msilamu** | "Usaonetsere kusangalala ndi kunyogodola pa tchimo la m'bale wako poti mwina Allah n'kumuchitira chifundo kenako iwe n'kukugwetsera m'mayerero". "Munthu amene anganyogodole m'bale wake ndi tchimo, sadzafa pokhapokha naye atachita lofanana nalo". |
| 34 | **Kukwiyirana pakati pa Asilamu awiri.** | "Sizili zololedwa kwa Msilamu kuti am'kwiyire m'bale wake kupitirira pa masiku atatu ndipo amene wam'kwiyira m'bale wake koposera masiku atatu, iye nafa, akalowa ku moto." |
| 35 | **Kuchita machimo mowonetsera** | "Ummat wanga wonse ukakhululukidwa kupatula iwo amene akuwonetsera machimo". |
| 36 | **Khalidwe loipa** | "Ndithu kuipa kwa khalidwe kumatheka kuononga ntchito yabwino monga m'mene viniga amaonongera uchi." |
| 37 | **Wolanda mtuka womwe waperekedwa kale** | "Wolanda mtuka womwe iye wapereka kale ali ngati galu amene akusanza kenako akubwereranso kudya masanziwo." "Sizili zololedwa kwa munthu kupereka mtuka kenako n'kubwereranso kulanda mtukawo." |
| 38 | **Kupondereza woyandikana naye nyumba** | "Atati munthu achite chiwerewere ndi amayi okwana khumi ndizopepuka kwa iye kuposa kuchita chiwerewere ndi mkazi wa munthu amene wayandikana naye nyumba. Ndipo atati abe munthu kuchokera ku nyumba khumi n'zopepuka kwa iye kuposa kuti akabe kuchokera kwa amene wayandikana naye nyumba." |
| 39 | **Kuyang'ana za Haraam** | "Zinalembedwa kwa munthu za gawo lake la chigololo kuti limenelo osalephera adzalipeza, pakuti maso chiwerewere chake ndiye kuyang'ana, makutu chiwerewere chake ndiye kumvetsera, lirime chiwerewere chake ndiye kuyankhula, mwendo chiwerewere chake ndiye kuyenda, ndipo mtima umagwa m'chikondi ndikusirira, ndipo maliseche amavomereza zimenezo kapena kukanira." |
| 40 | **Mwamuna kumukhudza mkazi amene sali halaal kwa iye.** | "Atati munthu abaidwe ndi singano yachitsulo m'mutu mwake kuli bwino kwa iye kusiyana ndikuti akhudze mkazi amene sali halaal kwa iye." "Ndithudi ine sindipatsana chanza ndi amayi". |
| 41 | **Ukwati wosinthana** | "Mtumiki (SAW) analetsa ukwati wosinthana." Kusinthanako ndiko kuti munthu akwatitse mwana wake wamkazi kwa munthu wina ndicholinga choti akwatire mwana wake wamkazi popanda kupatsana chiwongo. |
| 42 | **Kulira pa maliro mokuwa (mwamalumbo)** | "Amene waliridwa mokuwa ndiye kuti ameneyo adzalangidwa tsiku la Kiyaamat pa zimene analiridwa mokuwa." "Maliro amalangidwa m'manda ake pa zimene waliridwa mokuwa." |
| 43 | **Kuchilumbirira chosakhala Allah** | "Amene angachilumbirire chosakhala Allah ndiye kuti wachita ukafiri kapena shirk." "Amene angafune kulumbira ayenera kumulumbira Allah, |

| | | |
|---|---|---|
| | | kapena ayenera kuti akhale chete." |
| 44 | **Kulumbira kwa bodza** | "Amene walumbira popereka umboni kuti ndi kulumbira kumeneko adule chuma cha Msilamu pomwe iye ali wabodza pa chumacho akakumana ndi Allah atam'kwiyira iye." |
| 45 | **Kulumbira pogulitsa malonda** | "Pogulitsa malonda pewani kulumbiralumbira, chifukwa kulumbiralumbira kumachititsa kuti katunduyo agulidwe, kenako kumachotsa madalitso."<br>"Kulumbira kumachititsa kuti katundu agulidwe, kumachotsa madalitso." |
| 46 | **Wodzifananiza ndi makafiri** | "Amene wadzifananiza ndi anthu ena ake monga makafiri (anthu okanira Allah) ndiye kuti iye ndi mmodzi wa iwo."<br>"Sali mwa ife amene wadzifananiza ndi ena osakhala ife." |
| 47 | **Kumangira manda** | "Mtumiki (SAW) analetsa kuti manda achitidwe pulasitala ndi laimu, kuwakhalira ndi kuwamangira kanyumba". |
| 48 | **Chinyengo komanso kupusitsa** | "Allah akadzawasonkhanitsa anthu oyambirira ndi omalizira pa tsiku la Kiyaamat, mbendera idzatukulidwa ya aliyense wachinyengo ndipo zidzanenedwa kuti ichi ndi chinyengo cha uje mwana wa uje." |
| 49 | **Kukhalira manda** | "Kuti mmodzi wa inu akhalire khala la moto n'kuboola chovala chake n'kukafika pa khungu lake kuwawa kwake kudzakhala bola kwa iye kusiyana ndi chilango chokhalira manda." |
| 50 | **Amene akukondweretsedwa kuti anthu adziimirira iye akamabwera** | "Amene akusangalala kuti anthu adzionekera kwa iye chiliri, akonzekere za malo ake wokakhala ku moto". |
| 51 | **Kupempha popanda chifukwa** | "..... ndiponso munthu sangatsegule khomo la kupempha koma kuti Allah adzam'tsegulira iye khomo la umphawi." "Munthu amene apemphe anthu kuti achulukitse chuma chake, ndithu iyeyo akupempha khala la moto, choncho (zili kwa iye) achepetse kapena achulukitse." |
| 52 | **Kukwezerana mitengo mwa chinyengo** | "Mtumiki wa Allah (SAW) analetsa kuti munthu wokhala mu mzinda agulitse katundu wa munthu amene wachokera ku mudzi, udobadoba ngakhalenso kukwezerana mitengo mwa chinyengo, ndiponso asagulitse munthu pamwamba pa malonda a m'bale wake." |
| 53 | **Kulengeza mu Mzikiti kuti wataya kanthu** | "Amene angamumve munthu akulengeza kuti wataya kanthu mu mzikiti anene kuti: 'Allah asabwezere chinthucho kwa iwe', pakuti mizikiti sinamangidwire zimenezi." |
| 54 | **Kutukwana satana** | "Musatukwane Satana koma dzitchinjirizeni (kwa Allah) ku zoipa zake." Adayankhula mmodzi wa maswahaaba kuti ndidali pambuyo pa chokwera cha Mtumiki (SAW) ndipo nyama yakeyo idapunthwa ndipo ine ndidati: 'Satana waonongeka'. Ndipo Mtumiki (SAW) adati: "Usanene kuti satana waonongeka ndithu iwe ukanena zimenezo iye amadzikuza mpaka amafika kukula ngati nyumba nkumati: 'Oh ndikulumbirira mphamvu zanga!' koma udziti : 'Bismillah –mu dzina la Allah' ndithudi iwe ukatero amachepetsedwa kufikira amakhala ngati ntchentche." |
| 55 | **Kutukwana chiwawasa** | "(Iwe mkazi) usamatukwane chiwawasa ndithudi chiwawasacho chimachotsa machimo a mwana wa Adam monga m'mene chipala chimachotsera zoipa za chitsulo" |
| 56 | **Kufalitsa ndi** | "Ndipo amene waitanira ku zoipa adzapeza sambi zonga za amene |

| | | |
|---|---|---|
| | **kuitanira ku zoipa** | wachitsatira chinthucho, kuteroko sikudzapungula m'machimo awo kalikonse." |
| 57 | **Zoletsedwa pakumwa** | "Mtumiki wa Allah (SAW) analetsa kumwera kukamwa kwa mkunda kapena kwa kathumba ka madzi kachikopa."<br>"Mneneri (SAW) anazikalipira zakumwa madzi chiimire." |
| 58 | **Kumwera mu ziwiya za golide kapena siliva** | "Musamwere mu ziwiya za golide ndi za siliva, ndipo musavale nsalu za verevete ndi za siliki, pakuti izo ndi za iwo –makafiri- pa dziko lino lapansi, ndipo ku Aakhirat zikakhala zanu." |
| 59 | **Kumwera dzanja la manzere** | "Ndithu mmodzi wa inu asadyere dzanja lake lamanzere, ndiponso asamwere ndi ilo, pakuti Satana amadyera ndi kumwera dzanja lake lamanzere." |
| 60 | **Wodula chibale** | "Wodula chibale sadzalowa ku Jannat." |
| 61 | **Kusiya kumufunira zabwino Mneneri (SAW)** | "Yayaluka mphuno ya munthu amene ine ndatchulidwa pa maso pake ndipo iye sanandifunire zabwino."<br>"Waumbombo ndi amene ine ndatchulidwa pa maso pake napanda kundifunira zabwino. |
| 62 | **Kuweta galu** | "Amene waweta galu, kupatula galu wochitira liwamba, kapena kuyang'anira ziweto, pakuti kuweta galuko kumapungula m'malipiro ake maqeeraat awiri." |
| 63 | **Kuzunza ziweto** | "Analangidwa mayi wina wake chifukwa cha mphaka, anam'mangirira mpaka kufa, choncho analowa ku moto chifukwa cha mphakayo."<br>"Musachichite chinthu chomwe chili ndi moyo kukhala cholipsira ." |
| 64 | **Kuzipachika beru zifuyo** | "Angero satsagana ndi gulu lomwe mkati mwake muli galu kapena beru." |
| 65 | **Wochimwa akamapatsidwa mtendere** | "Ukaona Allah akupatsa kapolo za pa dziko lapansi zomwe akuzikonda iye pa machimo ake, kumeneko ndithu kumakhala kumuzamitsa kuchionongeko, kenako adawerenga kuyankhula kwa Allah koti: "Pamene adaiwala zomwe adakumbutsidwa, tidatsegulira iwowo makomo a zinthu zonse (zabwino) kufikira atasangalala ndi zomwe adapatsidwa, mwadzidzidzi tidawaononga iwono nakhala wodabwa." |
| 66 | **Kutsogoza duniya** | "Amene chingakhale cholinga Chake dziko lapansi, Allah adzauyika umphawi wake pamaso pake, ndipo adzalekanitsa mgwirizano wake, komanso sichingam'peza cha dziko lapansi kupatula chomwe chinakonzedwa kuti ndichake." |

# ULENDO WAMUYAYA NJIRA YAKO YA KU JANNAT KAPENA KUMOTO

**ALLAH AKUNENA KUTI: "E, INU AMENE MWAKHULUPIRIRA MUOPENI ALLAH NDIPO MUNTHU ALIYENSE ALINGALIRE ZIMENE WADZITSOGOZERA ZA MAWA"** (SURAT 59: 18).

**MANDA**: Iyi ndi nyumba yoyamba m'nyumba za ku Aakhirat, dzenje la moto kwa makafiri ndi achiphamaso, komanso ndi munda wamtendere kwa Msilamu. Ndipo zanenedwa kuti m'menemo muli chilango chifukwa cha machimo ena mwa iwo ndi awa: kusadzitalikitsa ku mkodzo, kukhwirizira nkhani, kuba katundu wa ku nkhondo, bodza, kugona osaswali, kuisamukira Qur'an, chiwerewere, matanyula, katapira, kusabweza ngongole ndi zina zotero. Ndipo zimene zingapulumutse ku chilangocho ndi izi: Ntchito zabwino zomuchitira Allah Yekha, kudzitchinjiriza mwa Allah ku chilango chake ndi kuwerenga Surat Al- Mulk ndi zina zotero. Ndipo amatetezedwa ku chilango chake: Shaheed, wolondera m'malire, womwalira tsiku la Jumuat, womwalira ndi m'mimba ndi ena otero.

## KUUZIRA LIPENGA

Lomwe ndi nyanga yaikulu mavuto ake, Mngero Israfeel (adaliyika pa kamwa pake) akudikirira kuti adzalamulidwa liti kuti aliyimbe ndipo Allah akunena kuti "Ndipo lidzaimbidwa lipenga, choncho amene ali kumwamba ndi pansi adzadzidzimuka kupatula yemwe Allah wamufuna". Choncho dziko lonse lidzaonongeka ndipo kutha kwa zaka makumi anayi lidzaimbidwa lipenaga la kuuka kwa akufa. Allah akunena kuti: "*Kenako lidzaimbidwa lipenga lachiwiri, pamenepo onse adzauka; adzakhala akuyang'ana modabwa*" (Surat 39:68)

## KUUKA KWA AKUFA

Kenako Allah adzavumbitsa mvula ndipo idzameretsa matupi kuchokera m'kafupa komwe kali kumapeto kwa fupa la munsana, ndipo chidzakhala chilengedwe chatsopano chopanda imfa, opanda nsapato kuphazi, amaliseche azidzawaona angero ndi majini, azidzaukitsidwa molingana ndi ntchito zawo.

## KUSONKHANA

Allah adzasonkhanitsa zolengedwa zonse kuti akaziwerengere ntchito zawo, zitagwidwa ndi mantha ngati anthu oledzera mu tsiku lalikulu, kutalika kwa tsikulo ngati zaka zikwi makumi asanu (50,000), zidzakhala ngati kuti pa dziko lapansi anakhala ola limodzi. Ndipo dzuwa lidzayandikira pa mtunda wa (1.5 km), ndipo anthu adzamira m'madzi a chitungu chawo molingana ndi ntchito zawo. Patsikulo anthu ofooka ndi odzitukumula adzakhala akukangana, ndipo kafiri adzakangana ndi mnzake, komanso Satana ndi mamembala ake ndipo adzakhala akutembererana, ndipo wopondereza adzakhala akudziluma manja ake, moto wa Jahannam udzakokedwa utamangiridwa zingwe zikwi makumi asanu ndi awiri (70,000), ndipo chingwe chilichonse chizidzakokedwa ndi Angero zikwi makumi asanu ndi awiri (70,000). Choncho kafiri akadzaiona Jahannam adzalakalaka kudziwombola kapena kusanduka dothi. Tsopano anthu onyozera okana kupereka Zakaat, chikayalidwa chuma chawo chili chamoto ndipo azidzaotchedwa nacho. Odzitukumula akasonkhanitsidwa ngati nyerere. Wonyenga, wakuba chuma cha kunkhondo, komanso wolanda, onsewo adzayalutsidwa ndipo wakuba

adzabweretsa chomwe anaba, ndiponso zidzaonekera zobisika. Koma omuopa Allah tsikulo silikawanjenjemeretsa ndipo likadutsa ngati Swalaat ya Zuhr.

## SHAFA'AT YOMWE NDI DU'AA YAIKULU YA MTUMIKI (SAW)

Idzachitika ndi Mneneri wathu yekha basi, kuzichitira zolengedwa pa tsiku losonkhana pa bwalo la mlandu kuti awachotsere mavuto awo ndi kuwawerengera ntchito zawo. Padzachitikanso Du'aa ya Mneneri (SAW) ndi anthu ena monga yowatulutsa anthu okhulupirira ku moto ndi kutukula maulemerero awo.

## CHIWERENGERO CHA NTCHITO ZAWO

Anthu adzaonetsedwa kwa Mbuye wao ataima mizeremizere, ndipo akawaonetsa ntchito zawo ndikuwafunsa za ntchitozo. Akawafunsanso za moyo womwe anali nawo, unyamata, chuma. Ilm ndi pangano, adzafunsidwanso za mtendere, kumva, kuyang'ana komanso mtima. Pomwe kafiri ndi mchiphamaso adzawerengedwa ntchito zawo pamaso pa zolengedwa zonse pofuna kuwayalutsa ndikuimika chigomezero pa iwo, ndikutinso anthu onse adzawaone. Adzafunsidwanso za nthaka, masiku, chuma, angero komanso ziwalo, kufikira zitatsimikizika ndi kuzivomera. Ndipo Allah adzakhala mwamseri ndi Msilamu ndipo adzavomerezedwa ndi machimo ake mpaka pamene iye adzaone kuti waonongeka, Allah adzamuuza kuti:"Ndinakubisira machimowa pa dziko lapansi ndipo Ine lero ndikukhululukira machimowo. Ummat wa Muhammad (SAW) ndi womwe udzayambirire kuwerengedwa ntchito zake, ndipo mwa ntchito zonse ntchito yoyambirira kuwerengedwa ndi ya Swalaat ndi kugamula milandu yokhetsa mwazi.

## KUULUZIKA AKAUNDULA

Kenako akauluzidwa akaundula ndiye adzikalandira kaundula (wosasiya chaching'ono kapena chachikulu koma kuchisunga), wokhulupirira akalandira ndi dzanja lake lamanja, ndipo kafiri komanso mchiphamaso adzalandira ndi dzanja lake lamanzere chakumbuyo kwake.

## SIKELO YOYEZERA NTCHITO ZA ANTHU

Kenako ntchito za anthu zikayezedwa kuti akawalipire nazo ndi sikelo yeniyeni yokhala ndi mbale ziwiri, ikalemeretsedwa ndi ntchito zogwirizana ndi Shariat zomusangalatsira Allah Yekha, ndipo mwa zina zomwe zikalemeretse sikeloyo ndi liwu loti LA ILAHA ILLALLAH, khalidwe labwino, Zikr monga kunena kuti AL HAMDU LILLAH NDI SUB - HANALLAHI WABIHAMDIHI, SUB - HANALLAHIL ADHWEEM. Ndipo anthu adzakhala akulipirana pa zomwe analakwirana popereka zabwino zawo kapena zoipa zawo.

## CHITSIME CHA MTUMIKI (SAW)

Kenako okhulupirira akafika pa chitsime, amene akamwe madzi wochokera mu chitsimemo pambuyo pake sadzamva ludzu mpaka kalekale. Ndipo Mneneri aliyense akakhala ndi chitsime, koma chitsime chachikulu kwambiri mwa zonsezo ndi cha Mtumiki Muhammad (SAW), madzi ake woyera kwambiri kuposa mkaka, otsekemera kwambiri kuposa uchi, onunkhira kwambiri kuposa mafuta a misk ndipo ziwiya zake chomwera ndi za golide ndi siliva ndipo zochuluka ngati nyenyezi, kutalika kwake ngati mtunda wochokera ku Ailat amene akupezeka ku Yorodani mpaka ku Edeni, madzi ake akuchokera mu mtsinje wa Kauthar.

## MAYESERO A OKHULUPIRIRA

Tsiku lomaliza pa bwalo la milandu makafiri azikaitsatira milungu yawo yomwe anali kuipembedza, motero ikawafikitsa ku moto ali m'magulumagulu ngati mdipiti wa zifuyo, akuyenda ndi miyendo yao kapena nkhope zawo, ndipo palibe akatsale pa bwalolo kupatula okhulupirira ndi achiphamaso ndipo Allah adzafika kwa iwo nati mukudikirira chiyani? Iwo adzati: "Tikum'dikirira Mbuye wathu ndipo anthuwo akamuzindikira Iye (SW) ndi katumba Wake akakam'vundukula ndipo akagwa kulambira kupatula achiphamaso, Allah akunena kuti: "*Akumbutse tsiku limene katumba wa Allah adzavudukulidwe ndipo adzaitanidwa kuti akalambire koma sadzatha kutero*". Kenako azidzamulonda Iye (SW) ndipo adzamanga mlatho ndikuwapatsa Noor anthu okhulupirira ndikuzimitsa Noor ya achiphamso.

## SWIRAAT

Umenewo ndi mlatho womwe waikidwa pamwamba pa Jahannam kuti azikaolokapo anthu okhulupirira popita ku Jannat, Mtumiki (SAW) anaulongosola kuti "*Mlathowo ndi woterera uli ndi mbedza zosiyanasiyana ngati minga ya mtengo wa kankhande wopyapyala kuposa tsitsi, komanso ndi wakuthwa kuposa lupanga*" **(Muslim)**

Ndipo pamenepo anthu okhulupirira adzapatsidwa noor (dangalira) molingana ndi ntchito zawo, amene adzapatsidwe noor (dangalira) yapamwamba kwambiri mwa iwo idzakhala ngati mapiri, ndipo amene adzapeza yochepetsetsa mwa iwo idzakhala pa nsonga pa chala chachikulu cha mwendo wake, motero idzakhala ikuwaunikira namaoloka pamlathopo molingana ndi ntchito zawo, choncho okhulupirira adzadutsa ngati kuphethira kwa diso, ena ngati mphenzi, ena ngati mphepo, ena ngati mbalame, ena ngati akavalo othamanga kwambiri, ena ngati ali pa chokwera, choncho pali amene adzapulumuke yemwe ndi Msilamu, ndipo wina adzangokandidwa n'kusiyidwa, pamene wina adzakokeredwa mu Jahannam **(Bukhaari,Mulsim).** Pamene achiphamaso sadzakhala ndi noor (dangalira), azidzabwerera, kenako pakati pa iwo ndi okhulupirira padzamangidwa mpanda, ndipo azidzafunitsitsa kuoloka mlatho ndipo adzakhala akugwetserana m'moto.

## MOTO

Akaulowa makafiri, kenako okhulupirira onyozera, kenako achiphamaso, pa chikwi chilichonse anthu (999) akaulowa, uli ndi makomo asanu ndi awiri, ndi oopsa kwambiri kuposa moto wa pa dziko lapansi kokwanira ka (70), kalengedwe ka kafiri m'menemo kakakhala kakakulu kuti akalawe bwino chilango, choncho pakati pa mapewa ake pakakhala potalikirana ngati mtunda woyenda masiku atatu, diso lake likakhala ngati phiri la Uhud, ndipo khungu lake likachindikala ndikumasinthidwa kuti akachilawe bwino chilango, chakumwa chawo ndi madzi ogaduka omwe azikawaduladula matumbo awo, chakudya chawo ndi Zaqqoom-mafinya osakanikirana ndi magazi komanso mafinya wamba. Mwa iwo amene adzapeze chilango chopepuka ndi amene adzaikidwe kunsi kwa mapazi ake makala awiri a moto, ubongo wake udzakhala ukuwira chifukwa cha makala amenewo, m'menemo muli kupserera makungu, kusungunuka, kuotchedwa kunkhope,

kukhwekhwerezedwa, maunyolo ndi magoli. Dzenje lake ndi lakuya kwambiri atati aponyedwe m'menemo mwana zitha kukwana zaka (70) kuti akafike pansi, nkhuni zake ndi makafiri komanso miyala, mpweya wake ndi mphepo yotentha, mthunzi wake ndi utsi otentha, chovala chake ndi moto, uzikadya chilichonse, choncho sukasiya kalikonse, uzikakalipa n'kumasokosera, ndipo uzikapsereza makungu komanso udzikafika m'mafupa ndi m'mitima.

## MLATHO (MGOGO)

Mtumiki (SAW) anati "*Okhulupirira akapulumuka ku moto, ndipo akaimitsidwa pa mlatho womwe uli pakati pa Jannat ndi moto, ndipo ena mwa iwo adzakhala akubwezerana kuponderezana kosiyanasiyana komwe kunalipo pakati pawo pa dziko lapansi, kufikira atayeretsedwa akaloledwa kulowa ku Jannat, choncho ndikumulumbirira Amene moyo wa Muhammad uli m'manja Mwake "Mmodzi wa iwo akawongoleledwa (akadziwitsidwa) za nyumba yake ku Jannat kuposa(momwe amaidziwira) nyumba yake ya pa dziko lapansi*." **(Bukhaari).**

## JANNAT (MUNDA WA MTENDERE)

Ndi malo wokafikira anthu okhulupirira, nyumba yake yomangidwa ndi siliva komanso golide, pulastitala yake ndi misk, miyala yake ndi ngale komanso miyala ya mtengo wapatali, ndipo dothi lake ndi Za'faraan ili ndi makomo asanu ndi atatu , khomo lake limodzi mulifupi mwake ndi motalika ngati mtunda woyenda masiku atatu, koma khomolo likathinidwa ndi chigulu. M'menemo muli masitepe (100), pakati pa masitepe awiri mpotalikirana ngati pakati pa kumwamba ndi pansi, pamwamba penipeni pali Firdaus, kuchokera m'menemo ikayenda mitsinje ndipo denga lake ndi mpando wachifumu wa Allah mitsinje yake ndi ya mkaka, uchi, mowa ndi madzi idzikayenda mosazama, okhulupirira azikaipatutsa m'mene adzafunire, zipatso zake zosatha zofupikira zopeputsidwa, yokungidwa ndi tenti yokhala ndi ngale mkati mwake mulifupi lake ndi mtunda wokwanira (60 mailosi), pakona iliyonse pali banja, anthu ake opanda tsitsi pa thupi, opanda ndevu, opakidwa wanja m'maso, chinyamata chawo n'chosatha ngakhalenso nsalu zawo, kulibe mkodzo ngakhale chimbudzi, ngakhalenso nyansi, zipeso zawo za golide, chitungu chawo ndi misk, akazi ake okongola, abuthu, achikondi ndi amuna awo, amisinkhu imodzi. Oyambirira kuilowa Jannatyo ndi Mtumiki Muhammad (SAW) ndi Aneneri. Ndipo mwa iwo amene akapeze Jannat yochepetsetsa ndi munthu amene akalakelake atapatsidwa Jannat, ndipo akapatsidwa ma Jannat khumi oonjezera, antchito ake ndi anyamata amuyaya, ooneka ngati ngale zomwazidwa, ndipo mtendere waukulu kuposa mtendere wake onse ndi kumuona kwa Allah kupeza chiyanjo Chake, komanso kukhalamo muyaya.

# KACHITIDWE KA WUDHU



**Sizikuloledwa kuchita Wudhu pokhapokha ndi madzi a Twahoor ndi womwe akadali mchilengedwe Chake, kapena amene asintha mtundu wake, kapena fungo lake, kapena kukoma kwake ndi chinthu cha Twahir, monga madzi osinthika chifukwa cha kukhalitsa kwake.** ✸ Ndi Makrooh kuchita wudhu ndi madzi ozizira kwambiri kapena otentha kwambiri, komanso kuyankhula mkatikati mwa Wudhu. ✸ Madzi ochepa akangokumana ndi Najisi amaipa, koma madzi ambiri monga okwana pafupifupi malitala (210) saipa, pokhapokha atasinthika mtundu wake, kapena fungo lake, kapena kukoma kwake.



**Ayambe kuchita Wudhu ndikunena Tasmiyah ndipo ndibwino kusamba m'manja pochita Wudhu ulionse, ndipo zikukakamizidwa kusambitsa manjawo katatu kwa amene akudzuka kuchokera mtulo ta usiku.** ✸ Akaiwala Tasmiya Wudhu wakewo watheka, ndipo akaikumbukira akuchita Wudhu anene Tasmiyah ndipo asayambirenso kuchita Wudhu. ✸ Sibwino kuonjezera pa katatu pochapa ziwalo zonse za Wudhu.



**Kenako achukuche mkamwa kamodzi, ndipo asalephere kugwedeza ndi kuzunguza madzi mkamwa, ndipo ndibwino kuchukucha katatu.** ✸ Kuchukucha sikungatheke pokhapokha ndi kachitidwe kanenedwaka ✸ Sizili Makrooh kumeza madzi pambuyo pochukucha. ✸ Ndibwino kuphatikiza pakati pa kuchukucha ndi kutsuka m'mphuno pogwiritsa ntchito chikhato chimodzi cha madzi, gawo lina la madziwo likhale lochukuchira, ndipo lotsalalo lotsukira m'mphuno.



**Kenako atsuke m'mphuno kamodzi ndipo asalephere kukoka madzi ndi mpweya kuti akafike mkati mwa mphuno n'kuwamina, ndipo ndibwino kuchita zimenezi katatu.** ✸ Kutsuka m'mphuno sikungakwanire pokhapokha ndi kachitidwe kanenedwaka. **ii.** Ndibwino kuthira madzi m'mphuno ndi dzanja la manja ndikuminira la manzere. ✸ Ndibwino kufikitsa madzi kum'mero pochukucha, komanso mkati mwa mphuno kwa amene sakumanga



**Kenako asambitse nkhope yake yomwe malire ake mulifupi ndi kuchokera ku khutu mpaka ku khutu lina, ndipo mulitali mwake ndi kuchokera momerera tsitsi la m'mutu mwachizolowezi mpaka ku chibwano.** ✸ Kutsanula ndevu n'kofunika ngati sizili zothinana ndipo ndibwino kuzitsanula ngati zili zothinana. ✸ Kupaka madzi kunkhope sikungakwaniritse kusambitsa. ✸ Ndibwino kutsogoza kuchukucha ndi kutsuka m'mphuno n'kumasambitsa nkhope, sibwino kuchapa mkati mwa maso pamene akusambitsa nkhope ✸ Ndibwino kuchulutsa madzi posambitsa nkhope mosakhala moononga.



**Kenako asambitse manja ake awiri kuchokera ku nsonga za zala pamodzi ndi akasukusuku.**
✸ Ndibwino kutsogoza kumanja ndikumalizira kumanzere posambitsa, ndinso kuwanyula manja awiriwo, ndibwino kusambitsa zikhato ziwiri poyamba kuchita wudhu, koma apapa ndipofunika ✸ Ndibwino kutsanula zala.



**Kenako apake madzi panja ponse pa mutu wake, kuyambira kutsogola kwake mpaka kunkhongo, kenako nkuwabwezera manjawo kutsogola kwa mutu, ndipo asasiye kalikonse m'mutumo, kuchokera m'malire mwa mutu mpaka kunkhongo, kenako alowetse zala zake ziwiri za mkombaphala momwe muli motseguka m'makutu ake ndikupaka madzi ndi zala zake ziwiri zazikulu zikulu kunja kwake mulimonse angapakire zidzatheka**
✸ Sizili Wajibu kupaka madzi tsitsi lomwe lazendewera ✸ Ngati mulibe tsitsi lipakidwe khungu la mutu. ✸ Ndipo osalephera kupaka malo oyera omwe ali pakati pa tsitsi ndi makutu, chifukwa iwo ali mkati mwa chinthu chotchedwa mutu. ✸ Sibwino kubwereza kupaka.
✸ Sibwino kutsuka tsitsi m'malo mopaka, koma kutsukako n'kokwaniritsa.



**Kenako asambitse mapazi ake awiri pamodzi ndi akasukusuku** ✸ Ndibwino kutsogoza kumanja ndikumalizira kumamzere, komanso kuwanyula **ii.** Ndibwino kutsanula zala

N'zofunikira kulondoloza pakati pa ziwalo za Wudhu, choncho adzayamba ndi kuchukucha, kutsuka m'mphuno kusambitsa nkhope, kenako manja awiri, kenako kupaka madzi pamutu, ndipo kenako kusambitsa mapazi awiri.
N'zofunikiranso kuwirikiza pakati pa ziwalozo, kotero kuti kusachedwetsedwe kusambitsa kwa chiwalo mpaka kuuma chiwalo chomwe chili m'mbuyo mwake.
**i.** N'zololedwa kupukuta ziwalo pambuyo pa wudhu, ndipo kusiya kupukutako ndibwino. Ndipo sibwino kusasa madzi a mziwalo.
**ii.** Wudhu sungatheke pochapa ziwalo zake zonse nthawi imodzi, monga kuti aimire mchitsime ndikuchita Niyyat ya Wudhu ndi Sunnah pambuyo pa Wudhu kunena Du'aa yoti **ASH - HADU AN LA ILAHA ILLALLAHU WAH DAHU LA SHARIKA LAHU, WA ASH - HADU ANNA MUHAMMADAN ABDUHU WARASULUH**, ndinso kuswali ma Raka awiri pambuyo pake.


# KASWALIDWE KA SWALAAT



**Akaimirira kufuna kuswali aiyambe Swalaatyo ndi mau ake onena kuti ," ALLAHU AKBAR." Imaam akweze mau ponena Takbirayo komanso ma takbira ena onse kuti amve amene ali pambuyo pake, ndipo amene Sali Imaam asakweze mau ponena Takbirayo, ndipo adzatukula manja ake zala zake zili zophatana pamene akuyamba Takbir moyang'anizana ndi mapewa ake, Imam akamaliza Takbirah yake naye Mamuma anene Takbir.** ✸ Ndi Wajibu kwa muthu amene akufuna kuswali kuti akhale atamalizika kuima pamene akunena Takbirah yoyamba, ndipo siingatheke kwa amene wawerama kapena wachikhalire kupatula kwa amene akulephera kuimirira ✸ Ndi Wajibu kukweza mau pa nsichi ndi chinthu cha Wajibu zoyankhulidwa mwa muyezo woti iye mwini amve ngakhale mu Swalaat ya chinsinsi, ndipo chinsinsi chochepetsetsa ndiye kudzimva munthu mwini wake. ✸Sibwino kutembenuka, kuyang'ana m'mwamba, kutsinzina ndi kuimirira atagwira m'mapewa kapena mchiuno kapena kuimirira ndi mwendo umodzi popanda chifukwa kapena kuphatanitsa mapazi awiri kapenanso kuwalekanitsa kwambiri monga zikuonekera mzithunzi zachiwiri.




**Ndipo dzanja lake la manja lidzagwira chikhato kapena pa malumi a chikhato cha manzere nawaika manjawo kunsi kwa chidale chake, ndipo maso ake adziyang'ana pa malo ake wochitira Sajdah. Kenako adzatsegula Swalaat ndi ma Du'aa ena omwe adza mu Sunnah, adzanena Ta'aw'wudh, kenako adzawerenga Tasmiyah, ndipo zonse zanenedwazi asakweze mau ponena. Kenako adzawerenga Fatihah, kenako adzawerenga paliponse pomwe angathe kuchokera mu Quràn ndipo Imaam pa Swalaat za Subh, ma Raka awiri oyambirira a Maghrib ndi Isha, adzakweza mau powerenga Quràn, ndipo mosakhala m'menemo adzanong'ona powerenga.** ✸ Ndi Makrooh kubwerezabwereza Fatihah mu Raka imodzi, ndiponso ndi Makrooh kungowerenga Farihah yokha m'ma Raka awiri oyambirira. ✸ Sizili Wajibu kwa Mamuma kuwerenga Fatihah m'ma Rakat okweza mau m'malo mwake udindo umenewo udzakhala ndi Imaam, koma ndibwino kuwerenga mamumayo Fatihah m'mene Imaam amakhala chete. ✸ Sizili Makrooh kubwereza Surah m'ma Rakat awiri, kapena kuigawa m'ma Raka awiri, ngakhale kuphatikiza ma Surah ambiri mu Raka imodzi, ngakhale kuwerenga kumapeto kwa Surah kapena pakati pake, kapena kumangowerenga Sura imodzi nthawi zonse, ali ndi chikhulupiriro choti kuwerenga Surah ina yosakhala imeneyo n'zololedwa. ✸ Ndibwino kuwerenga monga zilili mu msahafu ndondomeko ya ma Surah, ndipo ndi makrooh kutembenuza ndondomekoyo, ndipo zili Haraam kutembenuza ndondomeko ya mau, kapena ma Ayah omwe ali mu Surah imodzi.



**Kenako adzanena Takbir ndikutukula manja ake awiri n'kudzachita Ruku, ndipo adzaika manja ake awiri pa maondo ake kuchita ngati agwira, adzakanula zala zake adzaongola msana wake ndipo adzauika mutu wake molingana ndi msana wake, kenako anene kuti, "SUB -HANA RABBIYAL ADHWEEM." Ndipo zili Makrooh kungowerenga mauwa kamodzi, ndipo kukwanira konena mauwa mochepetsetsa ndiye katatu**

✸ Zili Wajibu kunena Takbir komanso mau oti SAMI - ALLAHU LIMAN HAMIDAH mkatikati mosamuka, ndipo sizikuloledwa kunena mauwa asanayambe kusamuka kapena atasamuka, chifukwa malo aliliwo ndi malo a zochitika zina ✸ Muyezo wokwanira kuti wachita Ruku, zimuthekere kugwira maondo ake awiri ndi zikhato zake ziwiri ndipo asachitire ulesi kapena kukokomeza pakuweramapo, monga zilili pa maonekedwe achitatu. ✸ Raka imapezedwa chifukwa cha Ruku, ndipo pasalephere imaam ndi Mamuma kukumana pa ruku'po asananyamule mutu wake kuti Raka imeneyi itheke. ✸ Wofunika kuswali akalowa m'Masjid Imaam ataweramuka pa Ruku ndibwino alowe naye ndikumtsatira, ndipo Raka imeneyo adzabweza ✸ Ndi Makrooh kuwerenga Quran pa Ruku ndi pa Sajda, pokhapokha ngati akufuna kuigwiritsira ntchito ngati Du'aa mwachitsanzo "RABBABA ATINA FIDDUN - YA HASANAH WAFIL AAKHIRAH"



**Kenako anyamule mutu wake akunena kuti," SAMI ALLAHU LIMAN HAMIDAH," ndipo adzatukula manja ake awiri choncho akakhazikika ataimirira anene kuti "RABAANA WALAKAL HAMDU, HAMDAN KHATHEERAN TWAIYIBAN MUBARAKAN FEEH, MIL - USSAMAWAATI WAMIL - UL - ARDHWI, WAMILU MA SHI'TA MIN SHAI - IN BAD."**

✸ Munthu woswali asanene Du'aa imeneyi pokhapokha ataimirira mokwanira pambuyo pa Ruku, asaiyambe Du'aayi asanaimirire, chifukwa malo ake ndi pambuyo pa kuimirira. ✸ Akaweramuka kuchokera pa Ruku ngati atafuna atha kugwetsa manja ake awiri, komanso ngati atafuna atha kuika dzanja lake lamanja pamwamba pa dzanja lake la manzere. ✸ Mau a Tahmeed alipo anayi, anatsimikizika kuchokera kwa Mnenenri (SAW) omwe ndi awa **1)** RABBANA WALAKAL HAMDU **2)**RABBANA LAKAL HAMDU **3)** ALLAHUMMA RABBANA WALAKAL HAMDU **4)**ALLAHUMMA RABBANA LAKAL HAMDU, Ndipo ndibwino kusinthasintha ponena mauwa.



Kenako adzapita pa Sajdah akunenaTakbir, ndipo adzalekanitsa manja ake osawagunditsa mnthiti zake, mimba yake osaigunditsa mntchafu zake, ntchafu zake osazigunditsa mu ake akatumba aka, ndipo adzaika manja ake awiri moyang'anizana ndi mapewa ake, ndipo nsonga za mapazi ake moyang'anizana ndi zala za manja ake komanso mapazi ake zitalunjika ku Qiblah. Kenako anene kuti "SUB - HANA RABBIYAL A'LA" ndipo ndi Sunnah kunena katatu. Akuloledwanso kuonjezera pa katatuko, kapena kupempha ndi ma Du'aa amene anadza kuchokera kwa Mtumiki.

✸ Ndi Makrooh kuyala manja pamene akuchita Sajdah, (monga momwe chimayalira chinyama cholusa. Monga zilili pa maonekedwe achisanu ✸ Kulekanitsa manja kuli bwino ngati sakumuvutitsa amene wagundizana naye ngati Sajdah yatalika akuloledwa kuti ayedzamire ndi akasukusuku ake powaika pa ntchafu zake. ✸ Ndi Wajibu kuti kukhale kusujudu ndi ziwalo zake zonse zisanu ndi ziwiri nsonga za mapazi ake, maondo ake awiri, zokhato zake ziwiri, komanso mphumi ndi mphumo. Ndipo Swalaat idzaononongeka ngati atasiya mwadala kusujudu ndi chimodzi mwa zimenezi.



Kenako adzanyamula mutu wake akunena Takbir ndikukhala. Ndipo kukhala kwa pakati pa ma Sajdah awiri kuli njira ziwiri zangwiro: **1)** Ayale mwendo wake wamanzere ndikuukhalira ndikuimika phazi lake lamanja ndikuzipindira zala zake kumbali ya qiblah **2)** Kuimika mapazi ake awiri ndipo zala zake zitalunjika ku Qiblah ndikukhalira zidendene zake. Ndipo anene kuti" RABBIGH - FIR - LI (katatu) ndipo akuloledwa kuonjezera ponena kuti "WAR - HAMNI, WAJ - BUR - NI, WAR. FA'NI WAR - ZUQNI, WANSUR - NI WAHDIN, WA - AFINI, WAFU ANNI." Kenako adzachita Sajdah yachiwiri ngati yoyambirira, kenako adzanyamula mutu wake akunena Takbir, ndipo adzadzuka akuimirira ndi zala za mapazi ake, choncho adzaswali Raka yachiwiri ngati yoyambirira.

✸ Pa Tashahhud ndibwino kuti adzichiyang'ana chala chake chakumanja chamkombaphala.
✸ Ndipo ndibwino pamenepa kusatalike kukhala kopitirira kukwanitsidwa kwa Attahiyaatu.



Ndipo akamaliza kuswali ma Raka awiri adzakhala kuti achite Tshahhud yoyamba mokhalira mwendo wamanzere ndipo adzaika dzanja lake lamanzere pa ntchafu yake ya manzere, ndipo dzanaja lake lamanja pa ntchafu yake yamanja, ndipo adzafumbata mzala zake za dzanja la manja chala chaching'ono ndi chotsatira chake, ndipo adzazunguza polumikiza chala chachikulu ndi chapakati ndikulozera ndi chala cha mkombaphala ndipo adzanena Tashahhud kuti "ATTAHIYAATU LILAAHI, WAS - SWA LAWAATU WATTWA IYIBAATU ....," Kenako adzadzuka mu Raka yachitatu ndi yachinayi akunena Takbir ndi kutukula manja ake, ndipo adzaswali ma Raka otsalawo monga zanenedwa kale, chabe kuti m'menemo sadzakweza mau ndiponso adzangowerenga Fatihah yokha basi.




Kenako adzakhala kuti achite Tashahhud yomaliza atakhalira thako, ndipo kukhala kumeneko kuli m'maonekedwe atatu angwiro. Ndipo asakhalire thako pokhapokha pakukhala komaliza mu Swalaat yomwe ili ndi ma Tashahhud awiri, kenako adzanena Tashahhud kuti "ATTAHIYAATU LILLAHI ......" kenako adzanena Swaliyatume ponena kuti "ALLAHUMMA SWALLI ALA MUHAMMAD WA ALA ALI MUHAMMAD ..... ". Kenako adzapempha chimene akufuna.

✸ **Maonekedwe a okhalira thako ndi awa: 1)** Adzayala pansi mwendo wa manzere ndikuutulutsa chakumanja kunsi kwa katumba wake, ndipo adziimika wamanja thako lake litagunda pansi. **2)** Maonekedwe ake omweo oyambirira koma adzayala mwendo wake wamanja. **3)** Maonekedwe ake omwewo koma adzaika mwendo wamanzere pakati pa katumba wake ndi ntchafu yake. ✸ Ndibwino kuti pamenepa apemphe ndi ma Du'aa ena omwe anadza, ndipo ena mwa iwo ndi awa AOODHU BILLAHI MIN ADHAABINNAR, WA ADHAABIL QABR, WAFITNATIL MAH - YA WAL MAMAATI, WAFIT - NATIL MASI HIDDAJJAAL, ndiponso ena mwa iwo ndi ALLAHUMMA INNI DHWALAMTU NAFSI, DHUL MAN KATHEERA, WALA YAGH - FIRUDH - DHUNUBA ILLA ANTA, FAGH - FIR - LI MAGH - FIRATA M'MIN IN'DIKA, WAR - HAMNI INNAKA ANTAL GHAFURUR - RAHEEM.



Kenako adzapereka salam ziwiri, motero adzatembenukira kumanja kwake akunena kuti "***Assalamu alaikum warahmatullah***," ndipo adzachita zimenezo chakumanja kwake. Akamaliza kupereka Salamu iye ali chikhalire pa malo ake woswalira adzachita Dua'a yomwe inadza kuchokera kwa Mneneri (SAW)

✸ **Ndibwino** kutembenuka pamene akupereka salam, ndipo adzapereka salam mbali yakumanja asanapereke kumanzere, ndipo ndi Makrooh kutsogoza kumanzere.

# ILM IMAFUNIKA KUIGWIRITSIRA NTCHITO

Ilm yopanda kuigwiritsira ntchito ndi yodedwa kwa Allah, kwa Mtumiki Wake ndinso kwa okhulupirira. Allah akunena kuti: "E, inu amene mwakhulupirira! BWANJI MUKUNENA ZIMENE SIMUCHITA? ALLAH AMAKUDA ZEDI KUNENA ZINTHU ZIMENE SIMUCHITA." **Abuu Hurairah** (RA) ananena kuti: "Chitsanzo cha Ilm yomwe sigwiritsidwa ntchito chili ngati chuma chosungidwa chomwe sichiperekedwamo pa njira ya Allah". **Ndipo Fudhail** (RA) ananena kuti: "Aalim adzakhalabe ali mbuli pa zomwe anaphunzira kufikira atazigwiritsira ntchito." **Komanso Malik bin Deenar** (RA) ananena kuti: "Udzampeza munthu sakulakwitsa chilembo china chilichonse, akamawerenga koma ntchito yake yonse ndiyolakwika".

**M'bale wanga wa Chisilamu, Mlongo wanga wa Chisilamu**

Allah wakupeputsira kuwerenga Buku laphinduli, ndipo kwatsala chipatso cha kuwerenga kwako chomwe ndi kugwiritsira ntchito matanthauzo a ma Ayahwa, omwe wawadziwa ,pakuti maswahaaba a Mneneri (SAW) anali kuphunzira kuwerenga ma Ayah khumi kuchokera kwa Mtumiki wa Allah (SAW), choncho sanali kuphunzira ma Ayah ena khumi mpaka atazindikira Ilm ndi ntchito zomwe zili m'ma Ayahwa, Maswahaaba anati: "Choncho anatiphunzitsa Ilm ndi ntchito, monga yalimbikitsira shariah kutero." Pa mau Ake (SW) onena kuti, "***Amaiwerenga kuiwerenga kwenikweni***", **Ibn Abbas (RA) adanena kuti mauwa** akutanthauza kuti akuitsatira kutsatira kwenikweni. **Ndipo Fudhwail (RA) ananena kuti:** 'Ndithu Quràn inavumbulutsidwa kuti igwiritsidwe ntchito, choncho anthu akuchita kuwerenga Quràn'yo kukhala ntchito.

Monganso yakudutsira Hadith ya Mtumiki (SAW) choncho chita changu kuvomera ndi kugwiritsira ntchito , pakuti ochita zabwino mu um'mah uno sanali kuphunzira kalikonse koma anali kuchita mpikisano pochigwiritsira ntchito ndi kuchiyitanira pofuna kukwaniritsa mau ake (SAW) onena kuti, "*Ndikakulamulani chinthu chichiteni m'mene mungathere, ndipo chimene ndakuletsani chipeweni*". **((Bukhaar), Muslim)**. Ndipo anaopseza chilango Chake chowawa m'mau Ake (SW) onena kuti, "***Achenjere amene amakana chilamulo Chake kuti ungapeze ukafiri kapena kuwapeza chilango chowawa***".

- Ndipo zina mwa zitsanzozi ndi izi; - Mayi wa Asilamu amene ali amake Habibah (RA) akunena Hadith kuti: "*Amene angaswali ma Rakat khumi ndi awiri usana ndi usiku, chifukwa cha ma Rakat amenewo adzamangiriridwa nyumba ku Jannah*." **(Muslim)**. Um'mu Habibah anati: "Kuyambira pamene ndinamva za ma Rakat amenewa kuchokera kwa Mtumiki wa Allah (SAW) sindinawasiyepo".
- **Ibn Umar (RA) akunena Hadith kuti:** "*Palibe ufulu wa munthu Msilamu amene ali ndi chinthu choti atha kusiyapo wasiya n'kugona masiku awiri pokhapokha wasiyawo ukhale utalembedwa kwa iye*."**(Muslim)**, Kenako akunena kuti: "Sudandidutseko usiku kuyambira pamene ndinamumva Mtumiki (SAW) akunena zimenezo koma ndimakhala nawo wasiya wanga".
- **Imaam Ahmad (RA) ananena kuti:** "Sindinalembepo Hadith pokhapokha nditaigwiritsira ntchito kufikira itandifika Hadith yonena kuti Mnenenri (SAW) anagwiritsa ntchito chiuwi n'kumpatsa abu Twayyibah dinar (ndalama), choncho ndinampatsa wouwika chiuwi Dinar imodzi pamene ndinagwiritsa ntchito chiuwi."

✱ **Imaam (Bukhaar) (RA) ananena kuti:** "Sindinajedepo aliyense ngakhale pang'ono kuyambira pamene ndidadziwa kuti kuteroko ndi Haraam.Ine ndikulakalaka kuti ndikakumane ndi Allah ndipo asakandipatse ine mulandu woti ndinamujedako wina wake".

✱ Mu Hadith mwadza mau onena kuti: "*Amene angawerenge Ayatulkurs; kumapeto kwa Swalaat iliyonse sichingamtsekereze chilichonse kukalowa ku Jannah pokhapokha atamwalira*"

✱ **Shaikh lbnul Qayyim (RA) anati:** "Anandipeza mau ochokera kwa Shaikhul Islam kuti iye anati: "Sindinaisiyepo Ayatulkursiyo kumapeto kwa Swalaat iliyonse pokhapokha moiwala kapena ndi zina zotero".

Ndipo pambuyo popeza Ilm ndikuigwiritsira ntchito pamayenereka kuitanira pa mtendere umene Allah wampatsa iyeyo ndikutinso usadzimane malipiriro ngakhalenso wina wake. Mneneri (SAW) ananena kuti: "*Amene walozera chinthu chabwino ndiye kuti nayenso adzapeza malipiro onga a amene wachita chinthucho*" (Muslim). Ananenanso kuti: "*Wopambana mwa inu ndi amene waphunzira Quràn, naiphunzitsa*" ((Bukhaar)), Mtumiki (SAW) anatinso: "*Perekani uthenga wochokera kwa ine ngakhale Ayah imodzi*." ((Bukhaar), Muslim). Ndipo pachifukwa cha kufalitsa kwako zabwino akuchulukira ndi kukulira malipiro , ndipo zabwino zako zikhala zikupitirira pamene uli moyo komanso pambuyo pa imfa. Mneneri (SAW) anati: "*Munthu akamwalira ntchito zake zopezera sawabu zimaima kupatula zitatu: sadaka yopitirira, monga kumanga mzikiti, kukumba chitsime ndi zina zotero kapena Ilm yomwe ikuwapindulira anthu, monga kuphunzitsa Ilm, kulemba zitabu ndi zina zotero, kapena mwana wabwino, wochita za Deen, yemwe angam'chitire Duàa iye* " (Muslim).

**KUUNIKIRA**

Timawerenga Surah Alfaatihah kambirimbiri kopitirira khumi kasanu nkawiri pa tsiku lililonse, m'menemo timadzitchinjiriza za anthu omwe anakwiyiridwa ndi Allah komanso za osokera, kenako timafanana nawo pa zochita zawo timasiya kuphunzira Ilm kuti tigwire ntchito mwa umbuli, motero timafanana ndi Akhristu osokera, kapena timaphunzira koma osazigwiritsa ntchito , choncho timafanana ndi Ayuda amene anakwiyiridwa.

Tikumpempha Allah kuti atipatse ife komanso iwe Ilm ya phindu ndi mphamvu yogwirira ntchito yabwino.

Allah ndi Mtumiki Wake ndi amene akuzindikira bwino lomwe, ndipo Allah apereke madalitso ndi mtendere Kwa Bwana Wathu, wokondedwa wathu Muhammad (SAW), akubanja lake komanso kwa Maswahaaba ake onse.

M’CHICHEWA

# تفسير العشر الأخير

من القرآن الكريم

ويليه

# أحكام تهم المسلم

www.tafseer.info